Maziko

Kumangilirika mu Chikhulupiliro

Kuyala Maziko pa Thanthwe, Yesu Khristu

Luka 6:48

Losindikizidwa ndi a

Village
Ministries
International

VillageMinistries.org

© 2001 by
Village Ministries International, Inc. (VMI)

VMI ikupereka mwayi kwa munthu wina aliyense kukopera ngakhalenso kugawa uthenga womwe uli mu maphunzirowa ndikugwiritsa ntchito yophunzitsa ena za Khristu ndi Mau a Mulungu. Komabe, munthu aliyense sakuloledwa kusintha, kuwonjezera kapena kuchepetsa uthengawu mwa njira ina iriyonse, ngakhale yochepa bwanji. Pozindikira kuti VMI imakhulupilira chisomo, potero munthu sayenera kuumirizidwa kuwerenga, kuphunzira kapena kugwiritsa ntchito maphunzirowa.

Kukopera, kufalitsanso, kugawa, kusindikiza kommanso kugwiritsa ntchito njira zina mwa zomwe ziri m'bukhumu ziyenera kuchitika mogwirizana ndi movomerezeka ndi ndondomeko ya maphunziro a Maziko amene akugwiritsidwa ntchito.

Copyright © 2001 Village Ministries International, Inc. Bukhuli linasindikizidwanso movomerezedwa.
Foundations ndilosindikizidwa ndi a Village Ministries International, Inc. VillageMinistries.org

Malemba onse a m'baibulo atengedwa kuchokera ku *New American Standard Bible*®, Copyright © 1960, 1962, 1963, 1968, 1971, 1972, 1973, 1975, 1977, 1994 by:

The Lockman Foundation
A Corporation Not for Profit
La Habra, CA

ZA MKATIMU

Kuthokoza **8**
Malonje **8**
Chaputala 1: **Kuyambapo** **9**
Gawo 1 Kudzikonzekeretsa 10
Gawo 2 Bukhu Lopatulika 12
Gawo 3 Mbiri, Mwachidule 15
Gawo 4 Zochitika mwatsatanetsatane 18
Gawo 5 Kukonzekera Kuphunzira Baibulo 22
Chaputala 2: **Kafukufuku Wa m'Chipangano Chakale** **25**
Malonje 26
Gawo 1 Mabukhu a Chilamulo: Mabukhu asanu oyambirira a m'Baibulo 28
Genesis 28
Eksodo 29
Levitiko 31
Numeri 32
Deuteronomo 34
Gawo 2 Mabukhu a Mbiri 36
Yoswa 36
Oweruza 37
Rute 39
1 Samueli 40
2 Samueli 42
1 Mafumu 43
2 Mafumu 44
1 Mbiri 46
2 Mbiri 47
Ezara 49
Nehemiya 50
Estere 51
Gawo 3 Mabukhu a Ndakatulo 53
Ndakatulo za Chihebri 54
Yobu 55
Masalimo 57
Miyambo 61
Mlaliki 62
Nyimbo ya Solomo 64
Gawo 4 Mabukhu a Aneneri Aakulu 66
Yesaya 67
Yeremiya 70
Maliro 71
Ezekieli 72
Danieli 74
Gawo 5 Mabukhu a Aneneri Aang'ono 76
Hoseya 77
Yoweli 78
Amosi 79
Obadiya 80
Yona 81
Mika 81
Nahumu 83
Habakuku 84
Zefaniya 84
Hagai 85
Zekariya 86
Malaki 87

Chaputala 3: Kafukufuku wa m'Chipangano Chatsopano 89
Mau Oyambilira 90
Gawo 1 Mabukhu a Mbiri 94
Mateyu 95
Marko 97
Luka 99
Yohane 101
Machitidwe a Atumwi 104
Gawo 2 Mabukhu a Mtumwi Paulo 106
Aroma 108
1 Akorinto 110
2 Akorinto 113
Agalatiya 114
Aefeso 115
Afilipi 116
Akolose 117
1 Atesalonika 118
2 Atesalonika 118
1 Timoteo 119
2 Timoteo 120
Tito 121
Filimoni 122
Gawo 3 Makalata Ena 124
Ahebri 124
Yakobo 126
1 Petro 127
2 Petro 128
1 Yohane 130
2 Yohane 131
3 Yohane 132
Yuda 132
Gawo 4 Bukhu la Uneneri 134
Chibvumbulutso 134
Chaputala 4: Ndondomeko Zenizeni za Kumasulira Mau 137
Malonje 138
Gawo 1: Funitsitsani kulandira mfundo yeniyeni ya Mulungu ndi Yesu pofunafuna malembo oyera 139
Mfundo 1: Kufunika kwa Mulungu 139
Mfundo 2: Funafunani njira yomwe Khristu Yesu waululidwamo 140
Gawo 2: Funafunani kumvetsetsa zoonadi pogwiritsa zofunikira pogwiritsa gawo lolondora la mlozo wanu 143
Mfundo 3: Zindikirani kuti bvumbulutso likupitilira 143
Mfundo 4: Masulirani momwe mwawerengera 144
Mfundo 5: Unikirani mfundo zofunikira 145
Lamulo 6: Phunzirani ndi kuchokera mu ndime zapaphata 145
Mfundo 7: Zindikirani za mphamvu ya munthu yopanga zinthu 146
Mfundo 8: Kumbukirani mapangano a Mulungu 147
Gawo 3: Funitsitsani Kupeza ndi Kukhala ndi pofananiza lemba ndi lemba linzake 151
Mfundo 9: Onetsetsani za kusiyanitsa 151
Mfundo 10: Unikirani za zinthu zimene zimachitika pamene ndime zimalembedwa 153
Mfundo 11: Masulirani Mofafaniza ndime 154
Mfundo 12: Funitsitsani kupeza umodzi wa ndime 155
Mfundo 13: Ganizirani za kusintha malinga ndi kusintha kwa nyengo 156
Mfundo 14: Chenjerani ndi uneneri 158

Gawo 4:	Funitsitsani Kukhala M'moyo wa Khristu Pogwiritsa ntchito bwino Mau a Mulungu	160
	Mfundo 15: Kugwiritsa Bwino Ntchito malemba zikutengera ndi Matanthauzidwe olondora	160
	Masitepe Asanu ogwiritsa ntchito Mau	160
	Zolepheretsa Zisanu Ndi Chimodzi pomasulira Mawu	161
	Njira zisanu ndi zitatu zolepheretsa kugwiritsa ntchito Mau a Mulungu	164
Chaputala 5:	**Chiphunzitso cha Umulungu**	**167**
Gawo 1:	Utatu Woyera wa Mulungu	168
Gawo 2:	Maina a Mulungu	172
Gawo 3:	Mulungu Atate (Chiphunzitso chokamba za Atate-Paterology)	175
Gawo 4:	Mulungu Mwana (Chiphunzitso cha Khristu- Christology)	181
Ndime 5:	Mulungu Mzimu (Chiphunzitso cha Mzimu Woyera-Pneumatology)	191
Chaputala 6:	**Chiphunzitso cha Kubala Zipatso mwa Mulungu**	**199**
Gawo 1:	Chilengedwe (Cosmology)	200
Gawo 2:	Angelo (Angelology)	201
Gawo 3:	Munthu (Chiphunzitso cha munthu-Anthrolopology)	207
Gawo 4:	Mkangano Pakati pa Angelo ndi Mulungu (Kuukira kwa Angelo)	217
Chaputala 7:	**Chiphunzitso cha Dongosolo la Umulungu**	**219**
Gawo 1:	Chibvumbulutso–Baibulo-(Bibliology)	220
Gawo 2:	Vuto: Tchimo (Harmartiology)	221
Gawo 3:	Yankho: Chipulumutso (Soteriology)	223
Gawo 4:	Chitezo: Malonjezo a Mulungu	227
Gawo 5:	Mtsogolo: Uneneri (Chiphunzitso cha zinthu za mtsogolo	230
Chaputala 8:	**Chiphunzitso cha Zolinga ndi Zokhumba za Mulungu**	**233**
Gawo 1:	Moyo wa UMunthu wa Khristu (Hodology)	234
Gawo 2:	Moyo womangililika wa Chikhristu	243
Chaputala 9:	**Kugwiritsa ntchito**	**247**
	Malonje	248
Gawo 1:	Kufuna kuzindikira bukhu	249
Gawo 2:	Muyenera kulongosola bukhu	250
Gawo 3:	Kuchepetsa Phunziro lowerenga	252
Gawo 4:	Kuyang'ana maubale kapena mg'wirizano wa mau	254
Gawo 5:	Kuunikira ndime	257
Gawo 6:	Kukuza zophunziridwa	259
Gawo 7:	Kulemba mfundo	262
Mawu Otsiriza		**263**
Mayankho		**264**
Ndandanda wa Mabukhu		**278**
Mathero		**279**

Kuthokoza

Maziko ndi maphunziro omwe akonzedwa pa upangiri wa Village Ministries International, Inc. Kuchokera pachiyambi, cholinga cha VMI ndichofuna kufikira midzi yonse yam'madera osafikidwa ndi uthenga wabwino wa Yesu Khristu. Kawirikawiri, mpata wa mamishonare umangopezeka kwa anthu ochepa komanso nthawi yochepa chabe. Choncho bungwe lathuli, cholinga chake ndi kufufuza ndi kupeza anthu omwe ali kumadera a kumidzi koma ali ndi mphatso ya utumiki monga ubusa, ulaliki, kapena uphunzitsi, ndipo tiwaphunzitse ndi cholinga choti iwowonso aziimire paokha ndikutha kupereka uthenga kwa anthu a mtundu wawo pokwaniritsa ntchiti "Yopanga ophunzira ku dziko lonse lapansi'' monga analamulira Ambuye Yesu Khristu.

Chaputala 2 ndi 3 chinatengedwa kuchokera ku chilolezo cha J. Hampton Keathley III's mu bukhu lake lotchedwa, ***The Concise Old and New Testament Survey.*** Ntchito yonse ya Bambo Keathley komanso imene siinaunikidwe mokuya mungathe kuipeza pa makina a internet kwaulere mogwirizana ndibungwe losachita phindu la Biblical Studies Foundation, pa: **www.bible.org**

Village Ministries International ikuthokoza Bambo Keathley pololeza kuti tigwiritse ntchito kafukufuku wawo. Ndime yakafukufukuyi ndi yofunika kwambiri mu maphunziro a Baibulo. Zina ndi zina tazikonza mu gawoli kuti lifanane ndi ndondomeko zophunzitsira mu Maziko makamaka masiku ndi zaka.

VMI ikukhulupilira kuti maphunziro a Baibulo awa akaperekedwa ku dziko lonse lapansi, makamaka kumadera omwe akufufukira kwambiri koma kulibeko. Kudzera mu utumiki uno, VMI yakwanitsa kuthandiza mwansanga kufikira azibusa a Madera akumidzi, komanso aphunzitsi ndi alaliki, ndi maphunziro awa omveka bwino komanso opindula.

Pali anthu ambiri omwe tikuwathokoza chifukwa cha kuzipereka kwawo pokonza maphunziro awa. Choyamba tikuthokoza Ambuye Yesu Khristu yemwe, mazisomo zake, watipatsa ife chipulumutso chachikulu ndi zonse zoyenerera ku moyo wa umulungu (2 Petro 1:3). Chachiwiri, pali anthu ambirinso omwe tikuwathokoza potpereka thandizi la kuthupi pokonza maphunzirowa kudzera mu mphatso, zipatso ndi kulolera kuti masomphenyawa atheke. Iwowa adwiradi ntchito yotamandika.

Mawu Otsogolera

Gawo la VMI la dongosolo lopereka mphamvu likutchedwa Maziko, yomwe lakonzedwa pofuna kuthandiza ophunzira atsopano a mawu a Mulungu kuti ***"Akule mu chisomo ndi chidziwitso cha Ambuye ndi Mpulumutsi, Yesu Khristu"*** (2 Petro 3:18). Choncho, kutsindika kwa Maziko sikuyenera kukhala ongomvedwa pofuna kuti ophunzira amve mawu ndi kukhonza mayeso ayi, komanso kuti athe kukula mu moyo wake wa uzimu.

Maziko akonzedwa pofuna kupereka mphamvu kwa ophunzira kuti athe kuphunzitsa anthu ena, pofuna kukwaniritsa mawu a Yesu oti "Pitani kudziko lonse lapansi …" pofuna kukwaniritsa utumikiwu (Mateyu 28:18-20).

Bukhuli liri ndi uthenga wofunikira omwe ophunzira mawu a mulungu ayenera kuwadziwa Chaputala 1, "kuyambapo'' likukamba za kufunika kozikonzekeretsa muuzimu ndipo potsatira likupereka mawu a Mulungu.

Chaputala 2 ndi 3, akulongosola mwachidule, kawuniwuni wa bukhu lirilonse la m'baibulo pofuna kupereka mfundo kwa ophunzira pa za mlambi ndi mfundo mu nkhani iriyonse, ndipo chaputala 4 chikumutsogoza ophunzira ku mfundo zofunika kwambiri zothandiza iye pa kumvesetsa mawu a Mulungu.

Chaputala 5 mpaka 8 chikulongosolera ophunzira za maphunziro a Umulungu, popereka maina ndi matchulidwe a mawu mu Baibulo, ndipo Chaputala 9 chikuphunzitsa ophunzira mmomwe angagwiritsire ntchito zomwe waphunzira ndi kuwerenga, pa kukonza phunziro loti aphunzitse kapena kulalikira.

Ndi pemphero langa kuti Maziko akuthandizeni kuti mumvesetse za Ambuye wathu Yesu Khristu, ndipo muyende mu chikhulupiliro povumbulutsiridwa mawu ake.

Takulandirani mu mawu ake Okoma-koma a Mulungu

Mutu 1

Kuyambapo

Gawo 1
Kudzikonzekeretsa

A. Mfundo Zisanu ndi imodzi Zomwe Wophunzira Mawu Ayenera Kutsatira

1. Khulupilirani mwa Yesu Khristu

Kudzikonzekeretsa musanayambe maphunziro a Baibulo sichinthu chonyozeka kapena chopanda pake. Choyamba, ophunzira ayenera kukhulupirira kuti Yesu Khristu ndiye Mpulumutsi wa moyo wake, chifukwa munthu wachithupithupi (wopanda Yesu) sangathe kulandira bwino kapena kumvesetsa bwino zinthu za Mulungu (1 Akorinto 2:14). Choncho, chipulumutso chimabwera pokhapokha ngati munthu akhulupilira mwa Khristu Yesu yekha (Aefenso 2:8-9). Ndipo akayamba kukhulupilira, Mzimu wa Mulungu amalowa mwa ophunzira ndi kupereka mzimu wachidziwitso ndi nzeru kuti athe kumvesetsa zinthu za uzimu.

2. Kuvomereza kuti Baibulo (Bukhu Lopatulika) ndilo Mau a Mulungu

Mawu a Mulungu amachitira umboni kuti ndi ouziridwa ndi mpweya wa Mulungu (2 Timoteo 3:16-17). Mu kuwerenga kulikonse kwa mawu a m'Baibulo, kuyenera kuyamba ndi chibvomerezo chakuti mawuwa ndi enieni, omwe Mulungu anawauzira ndi mpweya wake. Chikhulupiro chapakamwa chokha sichiri chofunikira; komano munthu akuyenera kukhulupilira kuti Baibulo ndi loona komanso lopanda chinyengo.

3. Kupemphera

Pemphero ndilofunika kwambiri kuti mudzimvesetsa mawu a Mulungu. Mawu amulungu amatilangiza kuti akasowa wina nzeru, napempha; Mulungu amupatsa iye kwaulere (Yakobo 1:5). Pemphero losweka mtima mtima lopempha nzeru zenizeni ndi mzimu wa chidziwitso lidzayankhidwa chifukwa zimenezi ndi zomwe Mulungu amafuna ndi kulingalira (1 Yohane 5:14; fananizaninso ndi Mateyu 7:7-8).

4. Phunzirani Mwachifatse/Osapupuluma

Pozindikira kuti nkhani zina za mu Bukhu lopatulika simungazimvesetse Pongowerenga kamodzi kokha, chifatso ndi chipiliro zikufunikira kwambiri kwa wophunzira mau a Mulungu (2 Timoteo 2:15). Nzeru za munthu zimakhala ndi malire, choncho muyenera kuphunzira ndi kukhulupilira kuti; ndi mphamvu ya Mulungu, chiri chonse ndi chotheka.

5. Bvomerazani Machimo Anu nthawi zonse

Ndikofunika kwambiri kuti mubvomereze machimo anu kwathunthu. Lolani Mulungu asule moyo wanu ndipo lolani kuti chiyanjano chachikuru chomwe chiri mwa Iye chilowe mumtima mwanu (1 Yohane 1:6-10). Kulapa mosweka mtima kudzathandiza kuti mukhale osinthika pa maganizidwe, mayankhulidwe, komanso ntchito zanu, molingana ndi chifuniro cha Mulungu.

6. Funitsitsani Kukhala m'chifuniro cha Mulungu

Ambuye Yesu Khristu anati, 'Ngati munthu aliyense afuna kuchita chifuniro chake, adzazindikira za chiphunzitsocho (Yohane 7:17). Ngati cholinga chanu chikhala chofuna kumanga ubale wabwino pakati pa in ndi Mulungu Wamoyo, chiphunzitso chirichonse chiyenera kulimbikitsa ndi kulongosola za ubale wanu ndi Mulungu. Chidziwitso chopanda chikondi; mathero ake ndi kudzikuza ndi kudzitukumula (1 Akorinto 8:1). Ngati cholinga chanu chiri chofuna kuphinzira zinthu izi monga zathupi, osati kupanga ubale ndi Mulungu Wamoyo, choncho chodziwitso chanu chikhala chosakhazikika komanso choonongeka.

B. Mapindu Asanu Omwe Amapezeka Pophunzira Mawu a Mulungu

1. Chikhulupiliro Chanu Chikula

Mtumiki wodziwika bwino anati ***"pakuti tiyendayenda mwa chikhulupiliro osati mwa maonekedwe"*** (2 Akorinto 5:7). Tonse tinalowa kuchipulumutso mwachisomo kudzera m'chikhulupiliro (Aefenso 2:8-9), ndipo Paulo anati: ***"monga momwe munalandira Yesu Khristu Ambuye, momwenso muyende mwa iye, ndi okhazikika m'chikhulupiliro monga munaphunzitsidwa, ndi kuchurukitsa chiyamiko"*** (Akolose 2:6-7).

2. Chidziwitso Chatsopano

Mumakhala chidziwitso chatsopano mu mawu a Mulungu ***"Kulani m'chisomo ndi chidzindikiritso cha Ambuye wathu Yesu Khristu"*** (2 Petro 3:15) chidzindikiritso chimenechi chimatitsogolera mu kuyamikira chisomo chomwe Mulungu waika kwa ife, komanso pamene chidzindikiritso chikula, ifenso timakula m'chikhulupiliro pamene timva mau a Mulungu kudzera mu malemba a m'bukhu lopatulika (Aroma 10:17), ndi kukhulupilira Mulungu nthawi zonse.

3. **Kuyeretsedwa kwa Moyo Wanu**
   Ndi mau a Mulungu okha amene angathe kuyeretsa miyoyo yathu chifukwa Iwo ndiwo mawu a choonadi (Yohane 17:17). Ngakhale Ife okhulupilira, nthawi zina timakhala m'mavuto mu miyoyo yathu (1 Yohane 1:6-10); choncho, tiyenera kuphunzira mawu a Mulungu kuti tizitha kusiyanitsa tanthauzo la tchimo, komanso zomwe zingatichimwitse. Pakutero, tingathe kupemphera mosweka mtima za machiritso ndi kuyeretsa (Masalimo 51), ndipo zizachitika monga momwe tapempha, chifukwa ndife oyera mtima. Zindikirani kuti akhristu ena awonjezera ziphunzitso zawo mu mawu a Mulungu m'dzina la chiyero. Izi ndi zilamulo komanso mfundo zakuthupi osati zauzimu. Anthu akuyesesa kupanga mfundo zawozawo zolungamutsa munthu mwachithupithupi, kuleka mfundo za Mulungu. Yesu Khristu anaona kale izi ndipo anatsutsana nazo (Marko 7:1-13). Choncho, tiyenera kukhala anthu ochenjera ndi atcheru pa nkhani, mau ndi ndondomeko za Mulungu.

4. **Mphamvu Mu Utumiki**
   Pamene tiwerenga mau, Mzimu Woyera akhala mkati mwathu makamaka pamene tiphunzira za malingaliro a Yesu Khristu (1 Akorinto 2:14-16), potero tizikhala ndi mphamvu zatsopano mu utumiki wathu (Aefenso 2:10). Zindikirani kuti tiri pankhondo ndi Satana mdierekezi ndi ankhondo ake; choncho tikusowekera kulandira mphamvu zachilendo zoposa mphamvu zathu zakuthupi, mphamvu zoposa malingaliro athu (Aefeso 6:10-18). Mphamvu zoterezi zimadza ngati tizipereka Kwa thunthu ku chifuniro chake cha Mulungu, chifukwa tikatero; Mulungu yekha ndi yemwe amagwira ntchito mwa Ife, ***"Pakuti wakuchita mwa inu kufuna ndi kuchita komwe, ndiye Mulungu, Chitani chonse popanda madandaulo ndi makani"*** (Afilipi 2:16).

5. **Kukonzekeretsedwa pa Utumiki**
   Kudzera mu maphunziro a mchidziwitso cha mau a Mulungu ophunzira akhala mumayendedwe achoonadi m'dzina la Ambuye wathu Yesu Khristu (Akolose 3:16-17), ndikutha kulengeza ndi kutumikira kwa osokera ndi akufa muuzimu a padziko lonse lapasi (Yohane 17:17-19; Ahebri 5:16) Cholinga choyambirira cha kulumikizina ndi mau a Mulungu ndicho "kukozdekeletsa oyera mtima kunthichito ya utumiki" kuwangirira mthupi la Khristu" (Aefeso 4:11-17). Tisanayambe kukonzekeretsa anthu ena, tiyenera kudzikonzekeretsanso ife eni.

Zoyenera podziyesa aliyense payekha: Mutu 1, Gawo 1

1. **Mau a chigiriki oti (psuchikos) za kuthupi opezeka mu 1 Akorinto 2:14 akupezekaso mu 1 Akorinto 15: 44-46; Yakobo 3:15 ndi Yuda 1:19 (ndipo mau amenewa atanthauzidwa monga "kulingalira za dziko". Werengani mabuku onsewa ndikupeza tathaunzo lenileni la za thupi.**

2. **Werengani 2 Timoteo 3:16-17. Tchulani mapindu anayi omwe akupezeka mu mawu a Mulungu? Kodi cholinga chake chiyani?**

3. **Pa Yakobo 1:15 kodi malonjezano kwa osowa nzeru ndi otani?**

4. **Werengani 2 Timoteo 2:15 kodi tiyenera kutani monga ophunzira a mawu a Mulungu? Kodi cholinga chathu ndichotani?**

5. **Werengani 1 Yohane 1:16-10, Kodi malonjezano awiri ati omwe aperekedwa kwa omwe avomereza machimo awo?**

6. **Yohane 7:17 akulongosola mfundo zolongosola za chifuniro cha Mulungu. Kodi mfundozi ndi zotani?**

7. **Werengani Akolose 2:6-7 ndi Aefeso 2:8-9, Tchulani zinthu ziwiri zomwe ziikulongosola makhalidwe a moyo wathu wa Chikhristu?**

8. **Werengani 2 Petro 3:14-18 Kodi ndi cholinga chotani cha Chikhristu Chomwe chikulongosola mu vesi 14 ndipo tchulani zinthu zomwe Zalongosola vesi 18 zomwe okhulupilira tiyenera kukula nazo Mu uzimu?**

9. **Bwererani ku Yohane 1:6-10. Tchulani zinthu ziwiri zomwe ndizofunika kwa okhulupilira kuti akhoze Kuyeretsedwa kumachimo ake.**

10. **Werengani Aefeso 6:10-18, ndipo tchulani adani enieni a munthu? Nanga tingamenyane nawo motani?**

11. **Werengani Aefeso 4:11-13, Tchulani zolinga zitautu "zomangira Thupi la Khristu."**

Gawo 2
Bukhu Lopatulika

A. Kodi Baibulo ndi Chiyani?

1. Baibulo ndi Mawu a Mulungu Olembedwa

Bukhu lopatulika siliri monga mabukhu ena awamba ayi. Ili ndilo mau a Mulungu lomwe analembedwa ndi anthu oposa makumi anayi omwe anakhalako ndi moyo padziko lino, zaka zoposa 1,500 (chikwi chimodzi ndi mazana asanu) zapitazo. Yesu Khristu analitchula Baibulo kuti ndi Bukhu (Ahebri 10:7). Popanda Baibulo, munthu sangathe kudziwa muyezo weniweni wofunika wa chikondi ngakhalenso kufunikira kwa Chisomo pa moyo wamunthu. Mulungu anasankha kuti pakhale mawu ake olembedwawa (Baibulo) ndi cholinga chakuti pakhale muyezo wa zinthu zomwe Iye akufuna kuti munthu azizichita ndiponso kuti zikhale zomveka ndi zodziwika bwino. Mau a Mulungu olembedwawa amavomerezedwa ndi munthu mwachikhulupiliro komanso potsimikizira ndi mbiri (izi ndi zinthu zomwe zachitika kale).

Munthu aliyense amamuyankhula Mulungu kudzera mu pemphero, koma Mulungu kawirikawiri, amamuyankhula munthu kudzera mu mawu ake olembedwa (Baibulo). Anthu ambiri amagwiritsa ntchito matanthauziro a Baibulo kuchokera kuziyankhulo zoyambirira za mawu a Mulunguwa, monga chihebri, chihelene ndi chi aranaiki. Gawo lalikulu la m'chipangano chakale linalembedwa m'chiyankhulo cha chihebri, kupatulapo bukhu la Danieli mutu 2 mpaka 7, ndi ukhu la Ezara mutu 4 mpaka 7. Mitu iyi ya Ezara ndi Danieli, inalembedwa mu chiyankhulo china chaching'ono chofananirako ndi chihebri chotchedwa Aramaiki chomwe chimayankhulidwa ndi kantundu kena ka chuyuda panthawi yomwe mabukhuwa ankalembedwa, koma chipangano chonse chatsopano chinalembedwa mchinenero chotchedwa KOINE kapena kuti chi Giriki (Greek)

Kugawa kwa mabukhu a m'Baibulo mu machaputala komanso mavesi zinapangidwa ndi anthu ouziridwa ndi mzimu Wa Mulungu, ndi cholinga chofuna kuti kukhale kosavuta kupeza, kuwerenga, ngakhalenso kufufuza nkhani a 'Baibulo. Kugawa kwa machaputala ndi mavesi kwathandiza kwambiri kuti kuzikhala kosavuta kumvetsa momwe magawo a nkhani akuphunzitsa kapena kutanthauza.

2. Baibulo ndi Mawu Owuziridwa ndi Mpweya Wa Mulungu

Lemba lirilonse la m'Baibulo linawuziridwa ndi Mulungu (2 Timoteyo 3:16-17) ndipo lipindulitsa. Kuuzira (mpweya wa Mulungu) ndi chinthu choposa monga momwe munthu angaganizire, ndiko kuwalitsa, komanso kubvumbulutsa, chifukwa izi zonse zinachitika motsogozedwa ndi Mulungu. Mpweya wa Mulungu unaperekedwa kudzera mwa munthu.

3. Baibulo ndi Bvubulutso la Mau a Moyo a Mulungu

Baibulo ndi bvumbulutso la mawu ake a Mulungu Wamoyo, Ambuye wathu Yesu Khristu. Mawu oti 'Bvumbulutso' amatanthauza kupereka uthenga watsopano kapena kuti 'Kuunikira' kumene kumachitika pamene Mzimu Woyera (womwe umagwira ntchito mwa iye), kumene kumapangitsa bvumbulutso kuti likhale lomveka bwino kwa wowerenga ndi wophunzira Mawu. Mawu olembedwa siali mau a Moyo; koma ndi mau okamba zimene anthu angatsatire zoperekedwa ndi Ambuye Yesu Khristu (Ahebri 4:12 komanso onani Yohane 5:39-47).

Izo ndizo mfundo zomwe muyenera kuzidziwa ndi kuzimvetsetsa bwino. Pepala ndi utoto (inki) pazokha ziribe mphamvu ina iriyonse ayi, koma mawu a Mulungu olembedwa papepala ndi utoto ndiwo omwe ali ndi mphamvu chifukwa cha Mzimu wa Mulungu ndipo mawuwa amabweretsa kusintha mu miyoyo ya wanthu. Choncho, kuoona ndi kungokhutira kuti mawuwa paokha ndi mwa iwo kuti ali ndi mphamvu popanda kudziwa za m'lembi wake, munthu amataya mfundo yeniyeni (Ahebri 12:2).

B. Dongosolo La Baibulo

1. Zigawo Ziwiiri Zazikulu za Baibulo

Baibulo lagawidwa mu zigawo zazikulu zikulu ziwiri: Chipangano chakale; Chipangano chatsopano

Muli mabukhu 66 mu Baibulo lonse. Mu chipangano chakale muli mabukhu 39, ndipo muchipangano chatsopano muli mabukhu 27, olembedwa ndi oposa 10 (khumi) Baibulo lonse liri ndi machaputula okwana 1,189. Mu chipangano chakale muli machaputala 929, ndipo mu chipangano chatsopano muli machaputala 260. Baibulo lonse liri ndi mavesi 23,214. M'chipangano chakale muli mavesi 7,959 pomwe chipangano chatsopano chiri ndi mavesi 31,173.

Pangano ndilo mgwirizano kapena kugwirira ntchito chinthu chimene chiri chofunikira kwambiri chimene chaperekedwa ndi munthu m'modzi chimene chimavomerezedwa ndi munthu wina. Mwachitsanzo,

ngati munthu akufuna kugula katundu, amauzidwa mtengo wake wakatunduyo, ndipo zimakhala kwa iye kuvomereza kapena kukana mtengowo. Pamene mtengo waperekedwa ndi kuvomerezedwa, pangano kapena mgwirizano (kontrakiti) umapangidwa pakati pa awiriwo. Mu chipangano mumakhala malonjezano ndi mfundo zolumikizitsa mbali zonse ziwiri malinga ndi zomwe amvana, kuvomereza ndi kulonjeza kuti achita. Chitsanzo chabwino cha pangano ndi malumbiro a 'ukwati woyera'. Malumbirowa amakhala mapangano ndi malonjezano pakati pa awiriwo, mkwatibwi ndi mkwati, pokhazikitsa maziko a chikondi chawo ndi moyo wawo watsopano wa m'banja.

Mu Chipangano chakale, muli mapangano enieni omwe Mulungu anapanga kwa munthu pokhudzana ndi kubwera kwa Mesiya (Mpulumutsi). Mtsogolo muno, pamaphunzirowa, tidzakambirana ndi kuunikira za mapangano amenewa.

2. Zigawo Zisanu ndi Chimodzi Za Muchipangano Chakale:

Chipangano Chakale chagawidwa motere:

a. Mabukhu a Chilamulo

Mabukhu a chilamulo kapena kuti Torah, muchiHebri kapena PENTATUECH mu Chihelene amatatanthauza mabukhku asanu. Mabubukhu a chilamulo m'chipangano chakale ndi awa: Genesis, Eksodo, Livitiko, Numeri ndi Deutoronomu.

b. Mabukhu a Mbiri

Pali mabukhu 12 (khumi ndi mphambu ziwiri) ambiri mu chipangano chakale. Mabukhuwa ndi ndi awa: Yoswa, Oweruza, Rute, 1 Samueli, 2 Samueli, 1 Mafumu, 2 Mafumu, 1 Mbiri, 2 Mbiri, Ezara, Nehemiya ndi Esitere.

c. Mabukhu a Ndakatulo

Awa ndi mabukhu asanu olembembedwa mwa ndakatulo. Mabukhuwa ndi awa: Yobu, Masalimo, Miyambo, Mlaliki ndi Nyimbo ya Solomo.

d. Mabukhu a Aneneri Akulu-Akulu

Mabukhu a aneneri akuluakulu alipo asanu, ndibo mabukuwa ndi: Yesaya, Yeremiya, Maliro, Ezekieli ndi Danieli.

e. Mabukhu a Aneneri Ang'ono-Ang'ono

Mabukhu a aneneri ang'ono-ang'ono mu chipangano chakale alipo khumi ndi awiri (12), ndipo mabukhuwa ndi awa: Hoseya, Yoweri, Amosi, Obadiya, Yona, Mika, Nahumu, Habakuku, Zefaniya, Hagai, Zekariya ndi Malaki.

3. Zigawo Zitatu Za M'chipangano Cha Tsopano

Chipangano chatsopano chimalongosola za kubwera Kwa Mesiya ndipo mu mabukhuwa mulinso mapangano omwe anakhazikitsidwa atabwera Mesiya padziko lapansi

Mu mabukhuwa mukumapezeka mabukhu ena a mbiri, ena momwe mkatikati mwakemo mulinso maulosi (mauneneri) monga (Mateyu 24, Marko 13, Luka 21). Chimodzi modzinso mabukhu enieni aulosiwo, mukumapezekanso makalata ena monga (Chibvumbulutso 2-3) Kasiyanisidwe kenikeni kodziwira mtundu kapena zigawo za bukhu lina liri lonse, chagona pa kumangilira ndi kumvetsetsa uthenga wonse womwe mutuwo ukunena. Chipangano chatsopano chagawidwa mu zigawo zinayi motere:

a. Mabukhu a Mbiri

Mabukhu asanu a mbiri mu chipangano chatsopano ndi awa: Mateyu, Marko, Luka, Yohane ndi Machitidwe a Atumwi.

b. Mabukhu a Makalata

Mabukhu a mbiri atsogozana ndi mabukhu a makalata. Mabukhu a makalata mu chipangano chatsopano alipo 21 (makumi awiiri ndi mphambu imodzi) Mabukhu a makalatawo ndi awa: Aroma, 1 Akorinto, 2 Akorinto, Agalatiya, Aefenso, Afilipi, Akolose, 1 Atesalonika, 2 Atesalonika, 1 Timoteyo, 2 Timoteyo, Tito, Filimoni, 1 Yohane, 2 Yohane, 3 Yohane, 1 Petro, 2 Petro, Ahebri, Yakobo, ndi Yuda.

c. Uneneri/ Ulosi

Bukhu la uneneri/ulosi mu chipangano cha tsopano ndi limodzi lotchedwa: Chibvumbulutso.

Mafunso odziyesa aliyense payekha: Mutu 1, Gawo 2

1. **Ahebri 10:1-7, Tchulani chinthu chomwe liwu lolembedwa silingathe kuchita palokha?**
2. **Ahebri 10:1-7, Kodi liwu lolembedwa linapangidwa kuti lizigwira ntchito yotani?**
3. **2 Timoteo 3:16-17, Kodi phindu la mawu owuziridwa ndi Mulungu ndi lotani?**
4. **2 Timoteo 3:17, Tchulani zolinga ziwiri za malemba opatulika (mawu a Mulungu/Baibulo)?**
5. **Yohane 5: 39-47, Kodi Yesu anawachenjeza motani anthu omwe akuphunzira mawu a Mulungu?**
6. **Kodi mbali yofunikira yeniyeni (kwambiri), ya mapangano kapena pangano ndi yotani?**
7. **Tchulani zigawo zisanu za mu chipangano chakale?**
8. **Kodi ndi kovomerezeka kuloza kapena kutchula aneneri aakulu ndi aang'ono monga aneneri wamba kopanda kuwasiyanitsa?**
9. **Tchulani zigawo zitatu za mu chipangano chatsopano?**

Gawo 3
Mbiri, Mwachidule

Kukoma kwa mawu a Mulungu kumadzindikiridwa ndi kudaliridwa chifukwa cha mchitidwe wake wosasintha sintha ngakhale kuti mawuwa analembedwa ndi anthu ambiri osiyanasiyana, kwa zaka zochuluka komanso zosiyanasiyana ndi zotalikirana zakalelo.

Ndandanda wa zochitika zofunika kwambiri womwe walembedwa m'musimu ukusonyeza ndikuchitira umboni malinga ndi momwe zinthu zinayendera. Poyang'ana zochitika zikuluzikulu tingathe kufufuza chiyambi ndi mathero a nkhani yonse yoyambayi ya mawu a Mulungu. Komaso tingathe kupezapo yankho lomveka bwino pa funso lomwe anthu ena anzeru za dziko la pansi (Filosofe) ofunafuna maganizo achidziwitso, akhala akumafusa nthawi zonse kuti "chifukwa chiyani anthu tili padziko"

Ndandanda uli mmusiwu unakonzedwa ndi cholinga cholongosola mwa chimvekere kwa ophunzira mawu a Mulungu kwa moyo wathu wonse tidzakhala tikugwilitsa ntchito tsatane tsataneyu. Kwa nthawi ino tiyeni tiphuzire mbiri zikulu zomwe Mulungu anaziika patsoglo pathu. Ndipo nthawi yina yam'tsogolo muphunziro lino, tidzaonanso ndandanda wokoma wa dongosolo lopambana losasinthika pa zochitika, la Mulungu.

A. Kalongosolodwe ka Zochitika

1. Chilengedwe

Kumayambiliro kwa Baibulo, Bukhu la Genesis lalemba za chilengedwe cheni cheni cha kumwamba ndi dziko lapansi (Genesis 1:1; 2 Petro 3:6). Kumapeto kwa bukhu la chibvumbulutso, chilengedwe chenicheni chaonongedwa ndipo njira ina yatsopano ya chilengedwe cha "Miyamba yatsopano ndi dziko lapansi latsopano yapangidwa" (Chibvumbulutso 21-22).

2. Kuwukira / Kugalukila) kwa Satana Mdierekezi

Kalekale munthu asanalengedwe, Satana anagalukila Mulungu (Yesaya 14:12-14; Ezekiel 28). Cholinga cha kuwukira koyamba kwa Satana kwalongosoledwa momveka bwino mu malemba, ndipo zotsatira zonse za kuukira kumeneku zimavuta kuzimvetsa bwino lomwe. Chimene chimamveka ndi chakuti pakhala pali nkhondo pakati pa Mulungu ndi Satana kuyambira pa nthawi imene munthu asanalengedwe (Chibvumbulutso 12) komanso kuti Satana adzaukilanso komaliza, pakatha zaka (1000) chikwi muulamuliro wa Yesu Khristu padziko la pansi, nthawi ya chilengedwe cha miyamba yasopano ndi dziko lapansi latsopano, isanafike (Chibvumbulutso 20:7-10).

3. Dziko lapansi ndi Munthu

Mulungu anakonza dziko lapansi ndicholinga choti munthu athe kukhalamo (Genesis 1:2– 2:3). Monga mwa mau ofotokozera za ndime omwe, mawu oti "opanda maonekedwe" MuChiHebri (TOHU) ndi mau oti "kupanda kanthu", (MuChiHebri-BOHU), kutanthauza kuti, "pamalo pamene sipangakhale anthu" komanso "anthu amene palibepo". Bvuto linalipo linali lakuti wina wolowelera, wina wowononga 'Satana,' yemwe amagalukira ndi kupikisana ndi Mulungu. Nthawi imene Mulungu adzamuika m'dende Satana kwa zaka chikwi (1000), munthawi ya mtsogolo ya ulamuliro wa Yesu Khristu, (Chibvumbulutso 20:1-3), Mulungu adzakhala akukonzanso dziko lapansi kuti likhale labambande ndilokongoletsetsa kukhalamo munthu (Yesaya 60-66).

4. Adamu Woyamba ndi Adamu Wotsiriza

Munthu woyambayo, Adamu anapangidwa kuti akhale munthu woyang'anira zolengedwa zones (Genesis 1:28; 2:4-25). Adamu anaikidwa m'munda wa Edeni kuti adzilima ndi kusunga za mundamo. Adamu wotsiza, Ambuye Yesu Khristu (1 Akorinto 15:45) adzakhazikitsa ulamulilo weniweni wooneka ndi maso pa dziko lapansi kwa zaka chikwi (1000) (Chibvumbulutso 2:4). Yesu Khristu ndiye "Chisanzo" podzindikira kuti palbie wina yemwe adzabwere ndikukhalopo wangwiro woposa Iye.

5. Nkhondo Pakati pa Munthu ndi Satana

Adamu atachimwa m'munda mwa Edeni, anasanduka kapolo wa Satana m'delekeza yemwe ndi olamulira zadziko lapansi (Genesis 3; Yohane 12:31; 61:11). Nthawi a mtsogolo. Usanafike ulamulilo wa zaka chikwi wa Yesu Khristu, Mulungu adzamtumize Satana kwa Khristu ndipo Satana adzamangidwa ndikukhala opanda mphamvu ndi ulamuliro (Chibvumbutso 20:1-3).

6. Kuweruzidwa kwa Munthu

Mulungu amavomereza munthu kulowa muuchimo, koma mtsogolo mwake adzathana naye munthu wochimwayo. Ku Genessis 4-10 tikupeza chiyambi chomwe chinachitisa kuti kubwere chigumula nthawi ya Nowa, chigumulachi chinachitika chifukwa cha kusakondwa kwa Mulungu komanso kuchimwa ndi kusamvetsa kwa anthu (Genesis 6:1-13). Mulungu adzanthananso ndi kulanga anthu ochimwa pamene

Yesu Khisitu adzabwelenso pa dziko lapansi, zitantha zaka zisanu ndi ziwiri zachitsautso chachikulu. Panhawi yonseyo, Mulungu anzakhala akulekanitsa anthuwo monga (nkhosa). Okhulupilira, ndi (mbudzi) osakhulupilira (Mateyu 25:31-46).

7. **Babulo**
Chitatha chigumula cha Nowa, m'dziko munakhalanso anthu ndipo anadzadza, koma posachedwa anthu anayamba kutsatanso zosalungama, kugulikira Mulungu. Anthuwa anamanga nsanja yaitali ku Babulo (Genesis 11) akuti pofuna kuti akamanga nsanja yaitali yofika kumwamba, adzabisala ku mkwiyo wa Mulungu (monga zinakhalira ndi chigumula ndi chombo cha Nowa), anthu ankaganiza kuti akatha kumanga nsanjayo ndikufika kumwamba, Maziko omwe amangapo nsanja yawoyi chinali chipembezo chija cha umunthu (Humanite) chomwe chimaphunzitsa ndi kukhulupilira kuti munthu angathe kuzipulumutsa yekha kudzera mu njira zachuma kapena zachipembezo. Zikhulupiliro ngati izi zafalikira kwambiri muzipembezo zambiri pa dziko lonse la pansi. Chipembezo cha chakhristu chokha ndichomwe chimaklupilira ndi kuphunzitsa kuti, munthu sangathe kudzipulumutsa kapena kudziwombola yekha ku mhwiyo wa Mulungu, koma pokha pokha kudzera mwa Mpulumutsi wathu Yesu Khristu. Makhalidwe achipembezo cha umunthu awonetseledwa m'malo ambiri m'Baibulo pamene akutsogolera za anthu omwe amaima ndi kumatsutsana ndi Mulungu wamoyo. Makhalidwe oterewa akupezeka Ku Baibulo wakale (Yesaya 47) ndi Tyre (Ezekiel 26-27) komanso makhalidwe oterewa akupezeka pakati pa anthu ngakhale masiku ano akupezekansomuzipembezo zambiri padziko la pansi zomwe zikukhulupililabe kuti munthu amatha kukwera udindo mpaka kufika pa Mulungu kapena woyera yemwe angathe kudzipulumutsa yekha. Pa nthawi ya "chisautso chachikulu," Mulungu adzawononga mabungwe ndi magulu a Ubabulo woterewu omwe akupezeka pa dziko lapansi (Chibvumbutso 17-18).

8. **Israyeli**
Anthu atabalalitsidwa kuchokera ku Babulo kudzera mukusokonekera kwa chiyakhulo, Mulungu anaitana Abrahamu ndikumupanga kukhala kholo ndi tate wamafuko ndi maiko (Genesis 12) kuzera mukubeleka mwana wake Isake kodziziswa, komanso Yakobo mdzukulu wake wa Abrahamu, malonjezano omwe Mulungu anaika pa Adamu a messiah (Mpulumtsi) anapitililabe (Genesis 22:1-18; 22:14). Anthu aku Israyeli anachotsedwa kuchokera ku dziko lawo ndikufalikira dziko lonse lapansi chifukwa cha mchitidwe wawo wopembeza mafano, komabe malonjezano a Mulungu pa munthu sanafe anaptililabe. Israel adzakhalabe wotoleledwa pamodzi mwa mphamvu zachilendo zauzimu ikatha nthawi ya "chisautso chachikulu" ndipo Israyeli adzadalitsidwa ndi ufumu wazaka zikwi ulinkudzawo (Mateyu 24:29-31).

9. **Kubweranso kwa Yesu Khristu**
Kubweranso koyamba kwa Yesu Khristu padziko lapansi kunachitika kale munyengo yake yoyikika ya Mulungu malinga ndi ndondomeko ya mbiri (1 Timoteyo 2:6). Uthenga wabwino wa Mateyu, Mariko, Luka ndi Yohane unalongosola momveka bwino za mbiri yozizwitsayi ya Yesu kuchokera kubadwa, utumuki, imfa, kuikidwa m'manda ndi kuukanso kwa akufa. Yesu Khristu anali mtumiki yemwe anavutika kwambiri yemwe nkhani zonse za masautso ake zinaloseledwa ndipo iye anadziziwa angakhale asanabwere padziko lapansi (Yesaya 53). Kubweranso kwachiwiri kwa Yesu Khristu kudzachitika zikatha zaka za "chitsauso chachikulu" pamene Yesu Khristu adzapondanso phazi lake padziko, ndikugonjetsa adani ake onse (Zekariya 14:1-8; Chibvumbulutso 19:11-19) ndicholinga chokhadzikitsanso ulamuliro wake wa zaka zikwi padziko lapansi latsopano. Panthawi imeneyi Yesu adzabwera ngati "Mfumu yogonjetsa."

10. **Mautumiki Otsutsa/Ogalukira**
Mabukhu authenga wabwino (Mateyu, Marko, Luka ndi Yohane). Utumiki wa Yesu Khristu unali wothandiza anthu ena (Mateyu 20:28). "Mwana wa munthu sanadza kutumikiridwa koma kutumikira, ndi kupeleka moyo wake, ndipo la anthu ambili." Utumiki wa Yesu Khristu ukutsutsana kwamphamvu ndi utumiki wa wokana Khristu (Antichrist) womwe umadziwikatso kuti (muthu wopanda lamulo) womwe ndi utumiki wongofuna kudziwonetsera kwa anthu kuti azikukonda ndi kukulambira (2 Atesalonika 2:1-12; Chibvumbutso 6:16).

11. **Mpingo**
Chitatha chiukitso ndi kukweranso kubwerera kumwamba, Yesu Khristu anakwezedwa nakakhala kudzanja lake lamanja la Mulungu Atate, ndipo mpingo unakhadzkisidwa kuti ufalitse uthenga wabwino wakukhululukira kwa machimo kudzera mu nsembe yomweYesu Khristu anapereka pololera kuzuzidwa, kupachikidwa, ndikuphedwa kwake (Machitidwe a tumwi). Mpingo uli ndi udindo wopanga anthu kukhala ophunzira a Yesu Khristu padziko lonse lapansi (Mateyu 28:18-20) mpakana mpingowo udzaitanidwa pa phwando la ukwati ndi Yesu Khristu mkwatiyo (1 Ateselonika 4:13-18; 1 Akolinto 15:50-58; Chibvumbulutso 19:7-10).

B. Chidule/Chindunji cha Nkhani Yonse

Tikaonesetsa ndikuunguza zochitika zonse zomwe zalongosoledwa pamwambazi, tikuona ndondomeko yomwe yakhazikitsidwa ndi Mulungu mododometsa kwambiri ndi ukadaulo wake. Ndondomekoyi yalukidwa bwino ndipo ikulongosoledwa mwachimvelekudzela mu chithunzichi. Makafanizila ma nambalawa amodzi, mudzaona ndondomeko yonse ya Mulungu yomwe iye anakhazikitsa kuyambira pachiyambi. Ndondomeko yonse mwachidule.[1]

1. Kulengedwa koyamba kwa kumwamnba ndi dziko lapansi (Genesis 1:1; 2 Petro 3:6)
2. Kugalukila koyamba kwa Satana (Yesaya 14:12; Ezekieli 28)
3. Dziko likonzedwa kukhala lokhalamo anthu (Genesis 1:2)
4. Utsogoleri WA Adamu woyamba (Genesis 2:4-25)
5. Munthu akhala pansi pa ulamuliro wa Satana (Genesis 3)
6. Kuweluzidwa kwa anthu (Genesis 4-10)
7. Kumanga nsanja ya Baibulo (Genesis 11)
8. Kutchulidwa Kwa Israeli kukhala dziko (Genesis 12)
9. Kubwera koyamba Kwa Yesu Khristu pa dziko (Mateyu, Marko, Luka, Yohane)
10. Utumiki wa Yesu (Mateyu, Marko, Luka, Yohane)
11. Kukhazikisidwa kwa mpingo (Machitidwa a Atumwi)
11. Kuitanidwa kwa mpingo (1 Atesalonika 4:13-18; 1 Akorinto 15:50-58)
10. Utumiki wa okana Yesu (2 Atesalonika 2:1-12; Chibvumbulutso 6–16)
9. Kubwranso kwa kwachiwiri kwa Yesu (Chibvumbulutso 19:11-19)
8. Kukonzedwanso kwa Israel (Mateyu 24:29-31)
7. Kuwonongeka kwa mabungwe a chibabulo (Chibvumbutso 17–18)
6. Kuwuzidwa kwa anthu onse (Mateyu 25:31-46)
5. Satana amangidwa maunyolo ndi Khristu (Chibvumbutso 20:1-13)
4. Utsogoleri wa adamu wotsiliza (Chibvumbutso 20:4
3. Kukonzedwa bwino kwa dziko lapansi (Yesaya 60–66)
2. Kuukira komaliza kwa Satana (Chibvumbutso 20:7-10)
1. Kulengedwanso kwa dzlko lapansi latsopano (Chibvu 21–22)

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Mutu 1, Gawo 3

1. **Genesis 1-2 ndi Chibvumbulutso 21-11. Ndipo munena zimene mawuwa akubvumbulutsa?**

2. **Yesaya 14:12-14 ndi Chibvumbulutso 20:7-10. Kodi ntchimo lenileni loyamba la Satana ndi lotani?**

3. **Genesis 1:2; Genesis 2:3; Yesaya 60-66 ku Genesis, dziko linapanGidwa labwino ndi loyera kukhalamo koma malinga ndi kuchimwa Adamu linasanduka lobvunda ndi loipa, kodi ndime ya mbukhu la Yesaya likulongosola zatani?**

4. **Genesis 3;1 Akorinto 15:45 ndi 1 Petro 2:22-24 kodi palikusiyana kotani pakati pa munthu woyamba Adamu, Adamu otsiliza yemwe ndi Yesu Khristu?**

5. **Aefeso 6:10-18, kodi adani athu enieni ndi ndani ndipo tingamenyane nawo motani?**

6. **Genesis 6:1-13 ndi Mateyu 25:31-46, Tchulani mutu wofanana mu nkhani za mabukhuwa?**

7. **Chibvumbultso 17-18 Chipembezo chachibabulo ndi chaumnthu (humanism) chimaphunzitsa kuti munthu angathe kudzipulumutsa yekha. Popanda kuwonera zomwe mabukhuwa alemba, tchulani njira ziwiri zomwe chipembezo cha Humanism chimaphunzitsa ndi kudzindikiridwa? (Chibvumblutso 17 ndi 18).**

8. **Genesis 12:1-3, Ahebri 11:8-12, Chibvumbutso 21:10-27 kodi lonjezo la Mulungu kwa Abrahamu lizakwanilitsidwa liti kwa munthu?**

9. **Yesaya 53; Zekariya 14:1-8; Chibvumbulutso 19:11-19 longosalani za kusiyana pakatipa kubwera koyamba kwa Yesu Khristu padziko lapansi kubweranso kwake kwachiwiri?**

10. **2 Atesonika 2:1-12; Mateyu 20:28. Tchulani kusiyana kwenikweni pakati pa utumiki wa Yesu khrist ndi utumiki wa okana Khristu (anti-christ)?**

11. **Mateyu 28:18-20; Machitidwe 1:8; 1 Atesalonika 4:13-18 tchulani ntchito yaikulu ya mpingo kufikila tsiku lomwe udzaitanidwa ndi Khristu?**

Gawo 4
Zochitika Mwatsatanetsatane

Ophunzira a mawu a Mulungu ayenera kuzindikira ndandanda, masiku, zaka komanso kulumikizana kwa nkhani zikuluzikulu zochituka zomwe zalongosoledwa bwino Baibulo. Gawo iri lalembedwa mwa dongosolo labwino komanso ndandanda wabwino potsata zochitikachitika zitatu zimenezi. Ndandanda woyamba tikunena ndandanda ya zochitika zikuluzikulu khumi zomwe zikupezeka m'buku lopatulika, masiku ndi zaka zomwe zinachitika komanso kumalizira ndi kufunia kwakwe kwa nkhaniyo. Ndandanda wachiwili ukulunjika pa zochitika zikulu zikulu zopezeka mu chipangano cha tsopano ndipo zikulongosola mabukhu omwe akukhudzana ndi zimenezo. Ndandanda wachitatu ukulongosola za zochitika zikuluzikulu zopezeka mu chipangano chatsopano.

Zaka zomwe zalembedwa "B.C." patsogolo pakezo zikutsonyeza kuti Yesu asanabadwe (Before Christ). Zaka zomwe zalembedwa "A.D." patsogolo pakezo zikusonyeza kuti Yesu atabadwa (Anno Domin, kuthauza kuti mchaka cha ambuye wathu Yesu Khristu).

Zaka zomwe zalembedwa mundime ino zachokera mu mawu a Mulungu.Anthu ambiri omwe anaphunzila za mawu a Mulungu anapeza zaka zosiyanasiyana. Musasokonezeke ayi ndime ino ndiyofunika kwambiri muphunzilori.

Maphunziro oyambilira omwe analembedwa kulongosola bwino za zaka 60 (makumi asanu ndi limodzi) omwe anatchulidwa pa Genesis 11:26, ndi Genesis 12:5 komanso anachitidwira umboni ku Matchitidwe Atumwi 7:4. Nkhani ya ku Machitidweyi imalongosola kuti Abraham anachokera ku Harana, Terah atamwalila. Terah anmwalira mu Haran ali ndi zaka 205 (ziwkizkwi ndi mphamvu zisanu) (Genesis 11:32), ndipo Abraham anacokera ku Haran ali ndi zaka 75 (makumi asnu ndi awiri kudza mphambu zisanu) (Machitidwe 7:4). Izi zikuthandauza kuti Terah anali ndi zaka 130 (zana limodzi ndi makumi atatu) pamene Abaham anabadwa zaka 70 (Makumi asanu ndi awili) zomwe zimanenedwa pa Genesis 11:26 zikhoza kumalongosola za kubadwa kwa Nahori kapena Harana (Genesis 11:28).

Ndikukhulupilira kuti izi zithandiza kulangiza ophunzira aliyense wa mawu a Mulungu kuti adziwerenga mabuku osiyana siyana am'Baibulo ndikufananiza kapena kutsimikizira nkhaniyo ndikuti pakuteropo nkhani yo imazitathauzira yokha.

A. Zochita Zikuluzikulu Khumi za M'bukhu Lopatulika ndi Zaka Zake

1. **Kuchimwa kwa Adamu (3958 B.C.)**
   Potanthauza za mibadwo molingana mawu a Mulungu, tonse tipeza kuti Adamu anachimwa mchaka cha 3,958 B.C. Ndondomeko ya nthawi za m'Baibulo yaperekedwa munjira yachindunji moti munthu angathe kuwerenga bwino poyamba ndi kulengedwa kwa Adamu kapenanso kuchokera pa chaka chachinayi cha ufumu wa Solomoni (Mafumu 6:1). Bukhu lopatulika limasonyeza kauniuni yense wa zaka zochitika zikuluzikulu. Ndipo ngakhale titalumikiza pa zomwe zachitika monga zanenedwera mu Mabukhu a pa dziko lapansi ndi zomwe Baibulo likulongosola pa mbiliyi, tingathe kuonanso kuti zakazi ndi zofanana ndithu.

2. **Chigumula cha Nowa (2302 B.C.)**
   Tikatsatira mibadwo yaku Genesis 5, tipeza zaka 1,656 zomwe zinapita kuchokera pakuchimwa kwa Adamu mu Edeni kufika pa nthawi ya chigumula cha Nowa.Ndipo izi zikutsimikiza kuti chaka cha 2303 B.C. chigumula chinachitika.

3. **Lonjezano la Mulungu kwa Abrahamu (1875 B.C.)**
   Mibadwo yomwe yalongosoledwa pa Genesis 11:12-26 ikulunjika kuti Adamu anabadwa zaka 352 kuchokera pomwe chigumula cha Nowa chinachitika, kapenanso kuti Abrahamu analandila lonjezano patatha zaka 2008 pambuyo pa Adamu. Izi zonse zikutsimikizira kuti Adamu anabadwa mchaka cha 1950 B.C.Timawerenganso kuchokera ku Genesis 12:4 kuti Abrahamu anali ndi zaka 75 (Makumi asanu ndi ziwiri kudza mphambu zisanu) pamene amalandira lonjezano lochokera kwa Mulungu kuti iye adzakhala Tate (kholo) wa mtundu ndi mafuko. Lonjezano la Abrahamu iri likusonyeza kuti Abrahamu analandiradi lonjezanoli m'chaka cha 1675 B.C.

4. **Ulendo wa Ana a Israyeli (1445 B.C.)**
   Genesis 12–50 amalongosola nkhani zokhudzana ndi mbumba ya Abraham ana a Yakobo (Chidzukulu cha Abrahamu) anayenda ulendo kusamukila kudziko la Aigupto ndipo pakupita kwa nthawi anasandisidwa kukhala akapolo a aanthu aku Aigputo (Eksodo 1). Chinankomera Mulungu kuwawombola ndikuwaturutsa ana a Israelwa kuchoka mu ukapolo wa Aigputo kudzera mdzanja la Mose. Bukhu la Agalatiya 3:17, ntumwi Paulo akulongosola kuti panatha zaka 430 kuchokera pomwe

Mulungu anapeka chilamulo kwa ana Israyeli kudzera mwa Mose. Chaka chomwe ana a Israyeli anachoka ku Aigupto ndi 1445 B.C. panali patatha zaka 2438 chilengedwere Adamu.

5. **Chaka Cha Chinayi cha Ulamulo wa Solomoni (965 B.C.)**
   Solomoni anali mfumu yachitatu kulamulira mtundu wa Israyeli iye anatsatira atate ake, ndipo Davide anatsatira mfumu Sauli. Pa 1 Mafumu 6:1, tikumva kuti panatha zaka 480 kuyambira nthawi yomwe ana aIsrayeli anachoka ku Aigupto (kupita ku Kenani) kufikira chaka cha chinayi cha ulamuliro wa mfumu pamene anayamba Solomoni kumanga Kachisi wa Yehova.alinga ndi nkhaniyi zinatisikizila kuti chaka cha 965 B.C. kapena kuti patatha zaka 2918 chilengedweni Adamu ndicho chaka chomwe Solomo anamanga Kachisi, atatha zaka zinayi pa Ufumu. Kuchokera pa chaka chimenechi, tingathenso kuwerenga mobwerera cha mbuyo kuti tipeze zaka zomwe anthu Israyeli anachoka ku Aigupto, kapena chaka chomwe kunali chigumula cha Nowa, ngakhaleso chaka chomwe Adamu anapangidwa.

   Nthawi zina mabukhu ena a padziko olongosola za mbiri akutchula zaka zosiyana ndi izi: zikhoza kuchitikadi motero cifukwa zaa zana limodzi (100) zapitazo anthu akala akusithasintha nkhani ndi zaka mwaupandu moti ziwakomere maliga ndi zokhumba zawo.Koma zaka zomwe talembazi ndizotsimikizika ndithu.

6. **Kugonjetsedwa kwa Ufumu wa Kumpoto (721 B.C.)**
   Atamwalira mfumu Solomoni, Israeli anagawikana kukhala maufumu awiri osiyana omwe amadziwika kuti ufumu wa kumpoto (Israyeli), ndi ifumu wa kumwera (Yuda). Ufumu wa kumpoto unagonjetsedwa ndi ufumu wa Asuri mchaka cha 721 B.C. ndipo ufumu wa Isreli (wakumptowo) unatheratu pomwepo.

7. **Kugonjetsedwa kwa Ufumu wa Kumwera (586 B.C.)**
   Ufumu wa kumwera (wa Yuda) unagonjetsedwa ndi ufumu wa Baibulo (Babylonian Empire) m'chaka cha 586 ndipo anthu anatengedwa ukapolo ku Baibulo kwa zaka 70 (makumi asanu ndi awiri), Ana a Israel asanaloledwe kubwerera kwawo mchaka cha 516 B.C.

8. **Kubadwa kwa Yesu Khristu (1 B.C.)**
   Zaka za B.C. ndi A.D. zinali zisanakhazikitsidwe mpaka kufikira m'zaka mazana asanu ndi limodzi 600, kuchokera pomwe Ambuye Yesu anakhala pa dziko lapansi. Zaka za B.C. ndi A.D. zinakhazikitsidwa polingana ndi ndondomeko ndi zaka zonse zambiri ndi kubadwa kwakwe kwa Yesu (Luka 1:5). Potsiriza panapezeka kuti kuphophonya kwa chaka chimodzi kapena ziwikumapezeka, komabe panthawiyi njilayi inali itakkhazikitsidwa ndikuyambaakudwila ntchito pachifukwa ichimmalo mositha zaka zonse zomwe zinali zitathazikitsidwa kale, kunachitika ganizo longopeka kuti Yesu anabadwa mchaka cha 1 B.C. kapena 2 B.C.

   Pali kusiyana pakati pa Kalendala ya Juliyo yomwe imayamba ndi 1 Januwale ndi kalendala ya Chiyuda yomwe imayamba ndi mwezi wa Sepitembala. Ichi ndicho chifukwa chake nthawi zina mupeza masiku ena amalembedwa mopenekera kuti "1-2 B.C." kapena "966-965 B.C."

9. **Imfa, Kuikidwa mmanda ndi Kuuka Kwakufa kwa Yesu Khristu (A.D. 32–33)**
   Ophunzira ochuruka a Baibulo anatchula tsiku la imfa, kuikidwa mmanda, ndi kuuka kwakufa kwa Yesu Khristu kuti chinari chaka cha A.D. 32–33.

10. **Bukhu Lomaliza la Baibulo (A.D. 96)**
    Chakachi chipezedwa polinganiza kuikidwa mdende kwa Yohane pa chisumba cha Patmo (Chibvumbulutso 1:9) munthawi yomwe mfumu yachiloma yotchedwa "Emperor Domitian" inali kulamulira, ndiyo nthawi yomwenso Baibulo linamalizidwaa kulembdwa (Chibvumbulutso 22:18-19).

B. Ndandanda wa Zochitika Zikulu Zikulumu Chipangano Chakale

1. **Kuchokera pa Adamu mpaka Chigumula Cha Nowa (3958-2302 B.C.)**
   Genesis 1–5

2. **Kuchokera Nthawi ya Chigumula Kufikira pa Lonjezano la Abrahamu (2303-1875 B.C.)**
   Genesis 6–12

3. **Lonjezo kwa Abrahamu ku Eksodo (1875-1445 B.C.)**
   Genesis 12–50; Bukhu la Yobu

4. **Kuchokera pa Eksodo Kufika pa Chaka Chachinayi cha Ufumu wa Solomoni (1445-965 B.C.)**

a. Eksodo	c. Numeri	e. Yoswa
b. Livitiko	d. Deutoronomo	f. Oweruza
g. Rute	i. 2 Samueli	k. 2 Mafumu
h. 1 Samueli	j. 1 Mafumu	l. 1 Mbiri

5. **Kuchokera Chaka Chachinayi cha Ufumu wa Solomo Kufika pa Kugonjetsedwa kwa Ufumu wa Yudah (965-586 B.C.)**

a. 1 Mafumu	g. Obadiya	m. Yesaya
b. 2 Mafumu	h. Yoweli	n. Nahumi
c. 2 Mbiri	i. Yona	o. Zefaniya
d. Miyambo	j. Amosi	p. Habakuku
e. Mlaliki	k. Hoseya	
f. Nyimbo ya Solomo	l. Mika	

6. **Nthawi ya Akapolo ku Baibulo (586-516 B.C.)**

a. Yeremiya	c. Ezekieli
b. Maliro	d. Danieli

7. **Utatha Ukapolo ku Baibulo, Mpaka Kutseka kwa Chipangano Chakale (516-400 B.C.)**

a. Ezara	c. Zekariya	e. Malaki
b. Nehemiya	d. Hagai	f. Estere

C. **Ndanda wa Zochitika Zikulu Zikulu za Mabukhu a Chipangano Chatsopano**

Mabukhu a chipangano chatsopano analembedwa, ndandanda molingana unagawidwa motere:

1. **Kuchokera pa Mbili ya Yesu Khristu, Mpaka Mbiri ya Mpingo Woyamba (A.D. 55-85)**

a. Mateyu	c. Luka	e. Machitidwa Atumwi
b. Marko	d. Yohane	

2. **Makalata a ku Mipingo (A.D. 46-85)**

a. Yakobo	h. Filimoni	o. Ahebri
b. Agalatiya	i. Aefeso	p. 1 Petro
c. 1 Ateslonika	j. Akolose	q. 2 Petro
d. 2 Atesolonika	k. Afilipi	r. Yuda
e. 1 Akolinto	l. 1 Tmoteyo	e. 1 Yohane
f. 2 Akolinto	m. 2 Tmoteyo	f. 2 Yohane
g. Aroma	n. Tito	g. 3 Yohane

3. **Uneneli / Ulosi (A.D. 96)**

Chibvumbulutso

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Mutu 1, Gawo 4

1. **Lembani Zochitikazi Mwa Ndondomeko Yolondola:**

Kutha Kwaufumu wa Kumpoto
Chigumula ChaNowa
Kutha kwa Ufumu wa Kumwera
Lonjezano kwa Ablahamu
Imfa Kuikidwa m'manda ndi Kuukanso kwa Kufa kwa Yesu Kristu
Ulendo wa Ana a Israel Kuchokera ku Eguputo
Chaka Chachinayi cha Ufumu wa Solomo
Kubadwa kwa Yesu Khristu
Kuchimwa kwa Adamu
Bukhu Lomariza la Baibulo

2. **Kodi ndi Mabukhu ati amchipangano Chakale omwe akunena za za pakati pa kulengedwa kwa dziko lapansi mpaka ulendo wa ana a Israyeli kuchokera ku Aigupto?**

3. **Lembani mabukhu amenewa mwandondomeko yake**

1 Samueli	Yoswa	2 Samueli
1 Mafumu 1-5	Deutoronomu	Livitiko
Numeli	Rute	Masalimo
Oweruza	1 Mbiri	Eksodo

4. Lembani mabukhu amenewa mwandondomeko yake

2 Mbiri	Yesaya	Hoseya
1 Mafumu 6-22	Nahumi	Yoweri
2 Mafumu	Amosi	Zefaniya
Miyambo	Mika	Habakuku
Mlaliki	Yona	
Nyimbo ya Solomo	Obadiya	

5. Lembani mabukhu amenewa mwandondomeko yake

Nehemiya	Ezekieli	Maliro
Danieli	Malaki	Hagai
Yeremiya	Ezra	
Estere	Zekariya	

6. Lembani mabukhu amenewa mwandondomeko yake

Mateyu	Luka	Machitidwa a Atumwi
Marko	Yohane	

7. Lembani mabukhu amenewa mwandondomeko yake

Aroma	2 Atesolonika	2 Petro
1 Akorinto	1 Timoteyo	1 Yohane
2 Akorinto	2 Timoteyo	2 Yohane
Agalatiya	Tito	3 Yohane
Aefeso	Filimoni	Yuda
Afilipi	Ahebri	Chibvumbulutso
Akolose	Yakobo	
1 Atesolonika	1 Petro	

Gawo 5
Kukonzekera Kuphunzira Baibulo

Mu magawo awiri apitawo tinali kulongosola za ubwino wodziwa nkhani zikuruzikuru zofunika zomwe zinachitika kale (Gawo 3) ndiponso ndondondomeko ya nthawi yomwe zinachitikira mwatsatanetsatane (Gawo 4). Pamenepa tikuyala maziko eni eni omwe adzakuthandizeni kuyankha mafunso omwe munthu amafunsa pameme akuphunzila za Baibulo. Funso lake limakhala "LITI" kapena kodi zinachitika liti? Pamene tikufunitsitsa kumvetsetsa za Baibulo, tipezanso kuti tiri kalikiliki kufufunza mafunso ndi mayakho omwe ndi ofunika ndi othandiza kuti tithe kugwiritsa ndi kulunjka nawo bwino mawu a Mulungu, omwe ndi mawu achoonadi (2 Timiteyo 2:15). Mulungu akutiitana tonse kuti tipite ndi mafunso onse kwa Iye (Mateyu 7:7-8) ndipo adzatiyakha.

Mafunso odziwikiratu omwe tingamafunse pamene tiwerenga Baibulo ndi awa: **ndani, bwanji, liti, kuti, motani** ndi **chiyani?** Mayakho amafunso oterewa ayenera kuganiziridwa pokumbukira mafunso awiri ofunika kwambiri pa moyo wathu wa chi Khristu. Kodi mawu omwe tawerengawa akuthandiza motani kuti tisendezere chifupi pauubale wathu ndi Yesu Khristu (Afilipi 3:10). Kodi ndingakhale bwanji (ndimoyo wa chiyelo) (Yohane 7:17).

A. Mafunso asanu ndi limodzi odziwikiratu pa vesi iriyonse

1. Ndani

Pofunsa funso loti "ndani" timafuna kuti tidziwe ndani yemwe akuyankhula ndipo akuyankhula kwandani mawuwo. Schitsanzo cha ku Genesesi 22:2 pamene Mulungu amamuuza Abrahamu kuti apereke mwana wake, mwana yekhayo Isaki nsembe yopsereza kwa Iye. Munkhaniyi tikuwona kuti Mulungu amayankhura kwa Abrahamu mwachindunji (masondimaso) osati kudzera mwamunthu wina. Choncho uthengauwu ndiwofunika kuti timve ndikutolapo nzeru koma osati tikuramulidwa kupereka ana athu nsembe yopsereza kwa Mulungu.

2. Chiyani?

Pofunsa funso loti "chiyani" tikufuna tdziwe choonadi chenicheni chomwe chikuyankhuridwa ndi chiyani. Yesu Khristu amafanizilidwa ku Chibvumbulutso 5 monga "mwana wankhosa" izi sizikutanthauza kuti iye anali waubweyaubweya kapena wamiyendo inayi ayi koma zoona zake za bvumbulutso limeneri ndilakuti zimangotanthauza za kudzipereka kwake kukhala nsembe yofera machimo athu (Yohane 1:29).

3. Liti?

Pofunsa funso "liti?" timafuna kuti tidziwe nthawi yomwe nkhaniyi inachitika mwachitsanzo ukwati wa Abrahamu kwa Sara mchemwari wake ukhoza kuwoneka ngati osayenera kufikira pamene owerenga angamvetsetse bwino kuti izi zinachitika zaka zakale Mose asanalandire malamulo khumi kuchokera kwa Mulungu. Malamulo omwe akutsutsana ndi mchitidwe wotelewu pozindikira kuti pamene palibe chiramulo palibe kulakwa (Aroma 4:15), komanso tikhonza kunena potengera ndi nkhani ya ukwati wa Abrahamu, iyeyo sanachimwe. Choncho funso loti "liti" ndilofunika kwambiri kuti ophunzira Baibulo kuti azindikire bwino ndikuphunzitsanso bwino ndi moyenera.

4. Kuti ?

Funso luti kuti? Limafotokoza za malo ndi dera lomwe nkhaniyo yachitikira. Kawiri kawiri mu Baibulo tikuwerenga mawu akuti kukwera ku Yerusalemu. Mawu amenewa mu zikhulupiliro zina akuoneka ngati akutanthauza kuti kuyenda kupita mpoto kwa Yerusalemu, koma malinga ndi Baibulo, mawuwa akutanthauza malo ukwera osati kuloza njira ayi. Pamene Yesu amachokera ku Galileya kukwera ku Yerusalemu, sizikutanthauza kuti Iye amapita ku mpoto ayi, amapita ku mwera koma kuti panali pamtunda, pa malo okwera.

5. Chifukwa Chiyani?

Funso loti chifukwachiyani ndirofunikila kwambiri kuyankha mafunso okuti kwambiri yankho nthawi za mmabukhu ena ngatimuwerenga Yesaya 7:14 ***"onani namwari adzaima nadzabala mwana wamwamuna ndipo adzamutcha dzina lake Emanueli,"*** funso lodziwikilatu likhale loti "chifukwa chiyani namwali" (wosadziwa mamuna) ndipo yankho lonveka bwino ndiroti,umu ndimomwe Mulungu anafuna kuti zichitike muona kuti yankholi ngakhale ndilolondola kwambiri, komabe ndilosatha, komanso losanvetsetseka tikamayangana mayankho, tipeza gawo la Aroma 5 lomwe limanena za zotsatira za uchimo wa Adamu pantundu wonse wa anthu.tipeza kuti kudzera kwa munthu mmodzi Adamu, munthu wina aliyense wachimwa choncho Yesu akanakhala ndi bambo ake a umunthu (apadziko, osati Mulungu atate), ndiye kuti iyenso akanababwa ndi tchimo lochokera kwa Adamu.

Choncho, poyankha funso loti: Chifukwa chiyani Yesu anabadwa mwa namwali (Virigo) Mariya yankho lake ndi lakuti; pamafunika kuti abadwe opanda tchimo kuti athe kupulumutsa anthu kuchokera ku tchimo lobadwa nalo lochokera kwa Adamu.

6. Motani/ Bwanji?

Funso loti, bwanji? ndi funso lovuta kwambiri. Tikhoza kufunsa, "Kodi zinatheka bwanji kuti ayende pamwamba pa madzi?" Yankho ndi lophweka lonena kuti izi zinatheka chifukwa Iye amadalira Mzimu wa Mulungu. Kodi Mulungu amalamulira mbiri pamene Iye wapereka ufulu wosankha kwa anthu? Funso ndi lovuta komabe tililondola bwino bwino ndikuliyankha mu phunziroli.

B. Mafunso Awiri Ofunika Kwambiri Pamunthu

1. Kodi zomwe ndawerenga zingathandize motani kuti ndisendeze chifupi ndikumanga ubale wabwino ndi Ambuye wathu Yesu Khristu?

Ili ndi limodzi mwa mafunso ofunikira kwambiri omwe wophunzira mawu a Mulungu ayenera kufunsa. Zimene ife taphunzira kudzera powerenga mau a Mulungu zayenera kulumikizidwa ndi chikhulupiliro (Ahebri 11:6) ndipo titatero, ubale wathu ndi Ambuye udzakula. Tiyenera kukhulupilira kuti mau a Mulungu ndi olondola komanso odalirika. Ndipo chotsatira chake tidzamanga ubale wabwino ndi Ambuye m'chikondi chake chomwe chiposa chikondi cha munthu. Mtumwi Paulo akunena mwachimvekere pa Aefeso 3:14-19:

> ***Chifukwa chake cha ichi, ndipinda maondo anga kwa Atate, amene kuchokera kwa iye pfuko lonse la m'mwamba ndi la padziko alitcha dzina,kuti monga mwa chuma cha ulemelero wake akulimbikitsani inu ndi mphamvu mwa mzimu wake, mkati mwanu; kuti Khristu akhale chikhalire, mwa chikhulupiliro mu mitima yanu; kuti odzika mizu ndi otsendereka m'chikondi, mukakhonzetu kuzindikira pamodzi ndi oyera mtima onse, kupingasa, ndi utali, ndi kukwera, ndi kuzama nchiyani; ndi kuzindikira chikundi cha Khristu chakuposa ma mazindikiridwe, kuti mukadzadzidwe kufikira chidzalo chonse cha Mulungu.***

Ngati tikungowerenga mawu a Mulungu ndikuwaphunzira ndi cholinga chongofuna kukhala ndi kuzama mu chikondi cha Mulungu, ndi chikondi cha pa anthu ena (Marko 12:29-31), ndiye kuti ndife oyerekedwa ndi amatama komanso opanda phindu. Pa 1 Akorinto 8:1 mtumwi Paulo yemwenso anali wodziwa kwambiri komanso wophunzira kwambiri maphunziro a za Mulungu koposa wina aliyense, (2 Akorinto 12:1-4), anaturutsa maganizo ake ndi zokhumba zake, poyankhula kuti: ***"Kuti ndimudzindikire Iye ndi mphamvu ya kuuka kwake, ndi chiyanjano cha zowawa zake pofanizidwa ndi inma yake; ngati nkhotheka; ndikafikire kuuka kwa akufa"*** (Afilipi 3:10). Pulo, monga mfarisi, anali wophunzira kwambiri, koma monga mkhristu, Paulo anayambanso kumanga ubale wake wabwino pakati pa iye ndi Mulungu Wamoyo.

Funafunani malonjezano a Mulungu, akhulupilireni, ndipo pakutero mudzakhala mu chisomo ndi chidziwitso mwa Ambuye wathu, Yesu Khristu (2 Petro 3:18).

2. Kodi Tingakhale Bwanji ndi Moyo?

Pamene tayamba kumvetsa tanthauzo la mawu opezeka mu vesi yomwe tawerenga, tiyeneranso tikhale ofunitsitsa kumvetsetsa kuti mawuwa atithandiza motani pa moyo wathu wa tsiku ndi tsiku. Mwa chitsanzo, pa Ahebri 12:1-3. Vesi 1 mpaka 2 ikuti:

> ***Chifukwa chake ifenso, popeza tizingidwa nawo mtambo waukuru wotere wa umboni, tiyenera titaye cholemetsa chiri chonse, ndi tchimoli limangotizinga ndipo tithamange liwiro, mwa chikhulupoiliro, makaniwo adatiikira, ndikupenyerera woyambirira ndi womalizira wa chikhulupiliro chathu. Yesu ameneyu, chifukwa cha chimwemwe choikidwa pamaso pake, anapilira mtanda, nanyozedwa, namchititsa manyazi, nafa, nadzuka kwa akufa, nakhala padzanja lamanja la ku mpando wachifumu wa Mulungu.***

Mlembi wa bukhu la Ahebri anagwiritsa ntchito chitsanzo cha masewera a mpikisano wothamanga; mu mavesi awiriwa. Pa mpikisano wothamanga amawerengera nthawi ndi kutalika kwa mtunda womwe wathamangidwawo. Anthu amakhala ndikumapenyelera mpikisanowo (Ahebri 11), ndipo wopambana pa mpikisanowu, amalandira mpando wa ulemu ndi mphoto. Olimbirana kuchita nawo mpikisanowu, amavula ndikuchotsa china chirichonse cholemera, powopa chingamulemere ndi kumuchedwetsa, ndikumulepheretsa kuchita liwiro loposa, kuti apambane pa mpikisanowo. Chomwechonso okhulupilira, ayenera kuika maso ako pa Yesu Khristu yemwe anapambana kale pogonjetsa imfa ndi zowawa, ndipo ali ndi moyo mpaka lero. Chikondwelero cha munthu yemwe wapambana, chimaposa komanso kukwirira zovuta ndi kutopa konse komwe anakumana nawo pa pa mpikisanowu.

Ndipo mu vesi 3 ya Ahebri 12, akuti:

> ***Pakuti tilingalira iye amene adalipira ndi ochimwa otsutsana naye, kotero kuti mungaleme ndi kukomoka m'moyo mwanu.***

Pamene tikumana ndi mayesero ndi mtsutso, zowawa, ululu, kuchititsidwa manyazi, kunyozedwa ndi kuyalutsidwa chifukwa cha Yesu Khristu, tiyenera kukumbukira kuti ngakhale Yesu mwini, anakumana nazo zimenezi, nazigonjetsa. Choncho ifenso, tiyenera kuchiyesa chimwemwe ndi chilimbikitso pamene tikumana ndi zinthu zotere. Ahebri 4:15 akuti ***"Pakuti sitiri naye mkulu wa ansembe wosatha kumva chifundo ndi zofooka zathu, koma wayesedwa mu zones monga mwa ife, koma wopanda uchimo."***

C. Kodi Chingachitike ndi Chiyani Ngati Sitingayankhe Mafunso Onse?

Mafunso onse ndiofunika kwambiri, chimodzi modzinso mayankho ake. Tiyenera kukumbukira kuti ubale wathu ndi Mulungu wamoyo, watheka kudzera mu chikhulupiliro. Aefenso 2:8-9 ***"Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo chakuchita mwa chikhulupiliro ndipo sichinachokere kwa inu, koma ndiyo mphatso ya Mulungu."*** Akolose 2:6-7 ***"Chifukwa chake monga momwe munalandira Khristu Yesu Ambuye, muyende howehonso wa Iye, ozika izu ndi omangilirika mwa Iye, ndi okhazikika m'chikhulupiliro, monga munaphunzitsidwa, ndi kuchurukitsa chiyamiko."*** Choncho, nkotheka kuti mwina sitingathe kupeza mayankho amafunso onse pa nthawi ino yomwe tiri ndi moyo, komabe Mulungu akutilonjeza ndi kutilimbikitsa kuti mafunso athu onse ali ndi mayankho ndipo Iye adzatiyankha (1 Akorinto 13:12).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Mutu 1, Gawo 5

1. **Werengani Yeremiya 39:1-2 ndipo muyankhe mafunso asanu ndi amodzi aja omwe timadzifunsa tikawerenga vesi iliyonse.**

   Ndani? =

   Chiyani? =

   Liti? =

   Kuti? =

   Chifukwa Chiyani? =

   Motani/ Bwanji? =

2. **Marko 12:29-31Tchulani zinthu zisanu zomwe zingapangise kuti tikhale opanda Ambuye?**

3. **Ahebri 11:6, 1 Yohane 2:7-11 Tchulani zinthu ziwiri zofunika kwambiri pamoyo wathu wa Chikhristu?**

Chaputala 2

Kafukufuku wa m'Chipangano Chakale

Malonje

Gawo lino ndi lamaphunziro mwachidule a kafukufuku wa mchipangano Chakale ndi Chatsopano. Cholinga chathu ndichofuna kupereka ndondomeko za mlembi, nthawi yomwe bukhulo linalembedwa, anthu ofunikira mu nkhaniya kapena kuti eninkhani, mutu wa nkhaniyi cholinga chomwe nkhaniyo yalembedwera komanso kulongosola momwe Yesu Khristu wafotokozedwera mu nkhaniyo.

Kafukufuku mwachidule wa bukhu linalirilonse mu Baibulo ndilofunika kwambiri kwa iwo amene akuphunzira Mau a Mulungu ndi cholinga choti amvetsetse bwino za zochitika zikuruzikuru ndi maphunziro a Baibulo. Izi ndizachidziwikire kuti pamene tiri ndi nthawi yophunzira mau a Mulungu, ndi pamenenso ife timadziwa zambiri za mauwo. Koma monga takhala tikuona mu maphunziro amenewa, ife tiri ofunitsitsa kuti poyamba tikhale ndi chithunzithunzi chachikuru kuti tikhonze kukhala ndi chidziwitso cha zinthu zina nthawi ina. Chaputala choyamba chiri ndi kauniuni wa Baibulo lonse. Ndipo chaputala chimenechi chikuyamba ndi kuonetsa mwachidule za bukhu lirilonse palokhapalokha.

Kufanizira Chipangano Chakale ndi Chatsopano

Yesu Khristu ndiye chiyembekezo komanso mutu waukulu mu nkhani zones za m'mbukhu la Baibulo. Nkhani zambiri, Yesu anadziulula yekha kuti iyeyo ndiye mutu kapena mwini Malembo a m'bukhu lopatulika (Baibulo).

1. Mateyu 5:17 Yesu anati, ***"Musaganizire kuti ndinadza ine kudzapasula chilamulo kapena aneneri, sindinadza in kudzapusula, koma kukwaniritsa."***
2. Yesu akuyenda ndi ophunzira ake pa msewu wopita ku Emawu, Luka amatiwuza kuti ***"Kuyambira nkhani za Mose ndi aneneri, ndi Masalimo; zonsezi zinalembedwa zokhudza Iye (Yesu)."***
3. Ndipo madzulo ake a tsiku limenelo, Yesu anayankhulanso ndi ophunzira khumi ndipo mlembi Luka analemba Luka 24:44-47 ***"Ndipo Yesu anati kwa akuphunzirawo, awa ndi mawu omwe ndinalankhula nanu, paja ndinakhala ndi inu, kuti ziyenera kukwaniritsidwa, zonse zolembedwa za ine mu mabukhu a mchilamulo cha Mose ndi aneneri ndi mmasalim."*** Ndipo anawatsegula mitima yawo kuti adziwe bwino malaembo, ndipo anati kwa iwo, ***"Kotero kunalembedwa kuti Yesu amve zowawa nauka kwa kufa tsiku lachitatu ndikuti kukalalikidwe m'dzina lake za kulapa ndi kukhululukidwa kwa machismo kwa amitundu yonse, kuyambira ku Yerusalemu."***
4. Mu Yohane 5:39 ndi 40, pokambirana ndi Ayuda, Yesu anati, ***"Musanthula malembo, popeza muyesa kuti momwemo muli moyo wosatha, ndipo simufuna kudza kwa ine, kuti mukhale nao moyo."***

Kuwonjezera apa, mu bukhu la Chibvumbulutso 19:10 tikumva kuti ***"Umboni wa Yesu Khristu ndiwo Mzimu wachinenero."*** Mwanjira ina, akufuna kufotokoza kuti, Mauneneri ndi malemba oyera akulongosola za Yesu Khristu. Mwachidziwikire, chifukwa cha kuchimwa kwa munthu, Khristu ndiye mutu wa nkhani mu mabukhu a m'chipangano chakale ndi chatsopano ndipo palibenso njira ina yomwe tingapezere moyo wosatha ndi moyo wochuruka, kuposa kwa Yesu. Ndadza ine kuti mukhale nawo moyo, ndikukhala nawo moyo wochuruka (Yohane 10:10).

Chipangano Chakale		
Chilamulo- Maziko a Khristu **Mbiri**-Kukonzekera Khristu **Ndakatul**o-Chikhumbokhumbo chofuna Khristu **Mauneneri**-Chiyembekezero mwa Khristu	Kukonzekera ndi Maziko ake	Chipangano chake chimayala maziko a kubwera kwa Mesiya, Mpulumutsi yemwe Amayembekezeredwa monga mneneri, wansembe, ndi mfumu monga yemwe adzalandire zowawa ndi kuphedwa, kufera tchimo la munthu, Iyeyo asanabwere kuzakhala ndi kulamulira dziko lapansi.
Chipangano Chatsopano		
Uthenga Wabwino (Mateyu, Marko, Luka, Yohane)	Kuchitira umboni (Chisonyez)	Mabukhuwa matidziwitsa nkhani za mabweredwea mpulumutsi woyembekezeredwayo (Yesu) pa dziko lapansi, ndi ntchito zomwe iye anazigwira
Machitidwe a Atumwi	Kukula kwa utumiki	Kudzera mu mphamvu ndi ntchito ya Mzimu woyera, bukhu la Machitidwe a Atumwi likufotokoza uthenga wa Mpulumutsi (Yesu), yemwe anabwera pa dziko lapansi.
Makalata	Kulongosola ndi Kugwiritsa ntchito Mawu	Akulongosola za kufunikwa kwambiri kwa Khrisu ndi mmene zingathandizire mkhristu kuti akhale kazembe wa Yesu Khristu pa makhalidwe ake.
Chibvumbulutso	Kumaliza (Mathero)	Akulosera ndi kunenera za m'masiku otsiriza ndi za kubweranso kwa Ambuye padziko, kulamulira kwake padziko, ndi moyo wosatha, kwa anthu.

Chidziwitso: Zindikirani kuti dongosolo lomwe talembali silinalongosole za bukhu lirilonse palokha palokha, kapena mutu wa m'bukhumo, kapena ndime (mavesi). Choncho inu ophunzira a mau a Mulungu mukufunsidwa kuti muwerenge gawo lina lirilonse, palokha ndipo mupeze mutu wake.

Gawo 1
Mabukhu a Chilamulo: Mabukhu Asanu Oyambilira m'Baibulo

Mabukhu asanu oyambirira mu Baibulo amatchedwanso PENTATEUCH. Mabukhuwa amadziwikanso kuti ndiwo mabukhu a chilamulo, chifukwa amalongosola za chilamulo ndi malangizo omwe Mulungu anapereka kwa ana a Isreali kudzera kwa mtsogoleri wawo Mose. Mabukhuwa analembedwa ndi Mose mwini, kupatulapo nkhani za kumatsiriziro a m'bukhu la Deutoronomu lomwe limakamba za imfa ya Mose. Mabukhu asanu a chilamulowa, amayala maziko a kubwera kwa Khristu, mwanjira yakuti Mulungu anasankha komanso kukhazikitsa mtundu wa Israeli monga mtundu wosankidwa wa Mulungu. Israyeli anakhala mwini ndi msungi weniweni wa m'chipangano chatsopano, wolandira mapangano a Mulungu komanso za Mpulumutsi (Aroma 3:2; 9:1-5).

Genesis
(Bukhu lokamba za Chiyambi)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Mlembi wa bukhuli ndi Mose. Mawu oti Genesis amatanthauza "Chiyambi," ndipo mawu a mu Genesis anatengedwa kuchokera ku mpukutu wa mawu womwe unatanthauziridwa kuchokera ku Chihebri kupita ku Chihelene (Septuagint).

Zaka: Bukhuli linalembedwa m'zaka za **1450–1410 B.C**.

Mutu ndi Cholinga: Ngakhale munthu atawerenga mwachidule, cholinga cha m'bukhu la Genesis ndicho chofuna kulongosola za madalitso ndi matemberero, kwa iye womvera Mulungu ndi Chikhulupiliro adzalandira mdalitso wa munda wa Edeni. Koma kwa munthu wosamvera, adzalandira themberero. Nkhani zones za mmbukhu la Mu bukhu la Genesis, lamangilirika pa mmadalitso kapena pa themberero. Komanso mutu weniweni ndi chisankho cha mtundu wa anthu kudzera mu kholo, Abrahamu yemwe analandira lonjezano. Mulungu anamulonjeza kuti adzamudalitsa, komanso adzadalitsa dziko lake (Genesis 12:1-3; Genesis 15:1-21).

Mawu oti Genesis, sakungotanthauza chiyambi chokha chabe ayi, koma akutanthauza "Ziyambi." Bukhu la Genesis likutipatsa nthano ndi mbiri zosiyanasiyana, ndi mmene Mulungu anazibvumbulutsira. M'bukhuli, nkhani ina iliyonse yaikulu, iri ndi chiyambi chake. Choncho, iri ndi bukhu la 'ziyambi' za nkhani zambiri. M'bukhuli muli chiyambi cha dziko lakumwamba ndi cha dziko lapansi, kupangidwa kwa munthu wa mwamuna ndi wamkazi, chiyambi cha tchimo pa munthu, chiyambi cha malonjezano a Mulungu kwa munthu, komanso chiyambi cha mtundu wa a Israeli womwe Mulungu anawusankha ndi cholinga choti kudzabadwira Mesiya ndi Mpulumutsi. Mu Genesis, tikuphunziramo za Adamu ndi Hava, za Satana M'diyerekeki, za Nowa, za chigumula, za Abrahamu, za Isaki, za Yakobo, za Yosefe ndi abale ake. Tikuphunziramonso za chiyambi cha ukwati, mabanja, kugawira ntchito, tchimo, kuphana, chilango kwa wakupha nzake, kuthira nsembe yopsereza, mitundu ndi mafuko, ziyankhulo, kupita patsogolo kwa mtundu wa anthu pa maganizo, (chikhalidwe ndi luso lapamwamba) (civilization), za sabata, za anthu a ku Baibulo ndi ganizo lawo lomanga nsanja ya Baibulo. Baibulo ndi bukhu lomwe limavumbulutsa mbiri zosiyanasiyana zomwe zinachitika.

Mawu omwe agwiritsidwa ntchito mowirikiza mu Genesis ndi oti, "Uwu ndi Mbadwo wa…" Mawuwa alembedwa kakhumi ndi mphambu imodzi (11), ndi cholinga chofuna kumulongosolera wowerenga pa ndime yotsatira yomwe iye awerenge pofananiza ndi zomwe zinachitika pa nkhani ina yambuyo, kuchokera nthawi ya kulengedwa kwa dziko, kulengedwa kwa anthu, komanso makolo onse a mtundu wa a Israyeli.

Anthu Mu Nkhaniyi: Adamu, Hava, Nowa, Abrahamu, Sara, Isaki, Rabeka, Esau, Yakobo ndi Yosefe

Khristu mu Bukhu la Genesis–Akuwonekera Mwa Ulosi/Uneneri: Munthu atangochimwa, lonjezano la chipulumutso linapatsidwa mwa mbewu ya mkazi (Genesis 3:15), ndipo lonjezano la kubwera kwa Mesiya lalongosoledwa mu bukhu lonse la Genesis: mbumba ya Seti, (Genesis 4:25), mphukira /mbewu ya Semu (Genesis 9:29), banja la Abrahamu (Genesis 12:3), mbewu ya Isaki (Genesis 26:3), ana a Yakobo (Genesis 46:3), ndi pfuko la Yuda (Genesis 49:10).

Pali mafungulo mu nkhani za m'bukhu la Genesis. Ndipo akulongosola za Mpulumutsi. **Adamu** akuyimilira Khristu (Aroma 5:14).

Adamu ndi mutu wa chilengedwacha kale, ndipo Khristu ndiye mutu wa chilengedwa chatsopano cha Mzimu.

Nsembe yopsereza ya **Abele** inali yoimilira kuti Khristu adzafera ife. Kuphedwa kwa Abele, kungathenso kuimilira imfa ya Khristu.

Melikizedeki monga mfumu komanso wansembe, akuimilira Khristu (Ahebri 7:3).

Yosefe yemwe anakondedwa kwambiri ndi atate wake, koma abale ake anamuda namugulitsa, kumapeto ake nakhala chiwombolo cha pfuko lawo, ndipo chiwombolochi chikuimilira Khristu.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

Perekani mitu ya nkhani yomwe ilibe mutu. Mu mituyo, mulongosole maubale pakati pa nkhani ina ndi inzake. Mwachitsanzo mu gawo "C" mutu ungathe kukhala:

1) Kukonzeka kwa Nowa pa Chigumula
2) Nowa m'chigumula
3) Chigumula
4) Pangano la Mulungu kwa nowa
5) Banja la Nowa

1. **Zochitika Zinayi (1:1–11:32)**
   a. Kulengedwa kwa dziko ndi munthu (Genesis 1:1–2:25)
   1:1–2:3 | 2:4-25
   b Kuchimwa kwa munthu (Genesis 3:1–5:32)
   3:1-24 | 4:1-24 | 4:25–5:32
   c. Chigumula/ kulangidwa kwa munthu (Genesis 6:1–9:29)
   6:1-22 | 8:1-22 | 9:18-29
   7:1-24 | 9:1-17
   d. Kumwazikana/kubalalika kwa mtundu wa anthu (Genesis 10:1–11:32)
   10:1-32 | 11:1-9 | 11:10-32

2. **Anthu Anayi: Kusankhidwa kwa mtundu ndi kukonzekera Muwomboli (12:1–50:26)**
   a. Abrahamu (tate wa chikhulupiliro ndikholo la mtundu wa Israeli) (12:1–23:20)
   12:1-20 | 16:1-16 | 20:1-18
   13:1-18 | 17:1-27 | 21:1-34
   14:1-16 | 18:1-33 | 22:1-24
   14:17-24 | 19:1-29 | 23:1-20
   15:1-21 | 19:30-38
   b. Isaki (Mwana wokondedwa wa lonjezano) (24:1–26:35)
   24:1-67 | 25:19-34 | 26:26-35
   25:1-11 | 26:1-17
   25:12-18 | 26:18-25
   c. Yakobo (Ndondomeko ndi kusunga ulemu) (27:1–36:43)
   27:1-46 | 31:1-55 | 34:1-31
   28:1-22 | 32:1-23 | 35:1-8
   29:1-35 | 32:24-32 | 35:9-29
   30:1-43 | 33:1-20 | 36:1-43
   d. Yosefe (Mazunzo ndi ulemelero) (37:1–50:26)
   37:1-36 | 40:1–41:57 | 49:1–50:21
   38:1-30 | 42:1–45:28 | 50:22-26
   39:1-23 | 46:1–48:22

Eksodo

(Bukhu la Chiwombolo)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Bukhu la Eksodo linalembedwa ndi Mose. Mawu oti Eksodo ndi a mu chilatini, omwe phata lake ndi lachihelene (Greek) "Exodos." Dzinali linaperekedwa pomwe amatanthauzira mpukutu wa mawu a Mulungu wa mu chihelene, ndipo Eksodo akutamthauza "Kuturuka."

Zaka: Bukhu la Eksodo linalembedwa mu zaka za **1450–1410 B.C.**

Mutu ndi Cholinga: Bukhuli liri ndi zolinga ziwiri: (1) Kuwomboledwa kwa anthu kudzera mu paskha; (2) Kuturutsidwa kwa ana a Ireaeli kuchokera mu ukapolo ku Agupto, ndi kuoloka Nyanja yofiira.

Patatha zaka zoposera mazana awiri (200) zakukura mu Aigupto, bukhu la Eksodo likufotokozanso za mtundu wa anthu osankhidwa, pfuko la Israeli ndipo likulongosolanso za kuwomboledwa kwawo kuchokera ku nkhanza za Aigupto komanso, kuperekedwa kwa chilamulo. Bukhuli limalongosolanso za kubadwa, kukhala, mbiri,

komanso kuitanidwa kwa Mose ndi Mulungu kuti atsogolere mtundu wake kuchoka ku Egupto kupita ku dziko lamalonjezano, dziko la Kenani. Ndipo kudzera mu paskha ya mwana wa nkhosa, kupululuka kwa ana oyambaa kubadwa kwa Aigupto, kudzera mu miliri khumi, komanso kuoloka kwa panyanja yofiira, Mulungu akuwonesera kuti Iye siwamphamvu zongoposa mfumu ya padziko monga Farawo kokha ayi, koma kuti Iye ndi Ambuye wopambana, waulamuliro wonse (YEHOVA), Mulungu wa chiwombolo, wamayankho komanso wa mabvumbulutso.

Anthu aja atatha kuoloka Nyanja yofiira, nafika mu chipululu, Mulungu anawapatsa malamulo ake a choonadi ndipo anawatchula kuti ndiwi anthu ake okundedwa omwe adzakhale ufumu wa ansembe, dziko loyera, umboni ku dziko lonse lapansi (Eksodo 19:4-7). Chilamulo choyera, kuphatikizapo malamulo khumi, chikutionetsera kuyera kwa Mulungu, kutiphunzitsa za momwa tingakondere Mulungu, komanso momwe tingakondere munthu mzathu, komanso mkatikati mwakemo, tikuonanso momwe anthu anamchimwira Mulungu ndi momwe Mulungu wakonzera dongosolo la chiwombolo, ndi kukhululukira kwa machismo. Dongosolo ili linaperekedwa kudzera mu LIKASA LA YEHOVA, nsembe zopsereza ndi nsembe.

Anthu: Mose, Aaroni, Miriyamu, Farawo

Khristu mu Bukhu la Eksodo: Pamene bukhuli likufotokoza mwachindunji zokhuza mauneneri okhuza Khristu, pali magawo angapo a upulumutsi mu bukhuli. Mu nkhani zambiri za mu bukhuli, **Mose** akuimilira Khristu. (Deutoronomu 18:15) akutiwonetsa kuti Mose, monga mneneri, ankayimilira Khristu. Kufanana pakati pa Mose ndi Yesu kunali kwakuti onsewa analolera kuwombola anthu, anataya mphamvu zawo kutumikira ena, kugwira ntchito ngati ankhalapakati, komanso ngati owombola anthu.

Paska ndi chizindikiro chapadera chomwe chimalongosola kuti Khristu anali mwana wankhosa wa Mulungu, wopanda banga kapena tchimo (Yohane 1:29, 36; 1 Akorinto 5:7).

Phwando lirilonse mwa maphwandowa, limayimilira chinthu china chake chokhuza Mpulumutsi.

Eksodo payokha, monga momwe Paulo amaluimkizitsa ndi ubatizo ikutipatsa chithunzi thunzi kwa ife kuti timzindikire Khristu kudzera mu imfa yake, kuikidwa kwake m'manda, ndi kuuka kwake kwa akufa (1 Akorinto 10:1-2; Aroma 6:2-3).

Mana ndi Madzi akuperekanso chithunzi cha Khristu (Yohane 6:31-35, 46-63; 1 Akorinto 10:3-4).

Likasa la Yehova likulongosolanso za Mpulumutsi kudzera mu zinthu zooneka ndi maso. Mtundu, zipangizo, masanjidwa a zipangizo, komanso nsembe zopsereza, ndi zoperekedwa (Ahebri 9:1–10:18).

Wansembe wa mkullu akutiunikira za umunthu komanso umulungu ndi utuimiki wa Khristu (Ahebri 4:14-16; 9:11-12; 9:24-28).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndomdomeko mwachidule

1. **Kuomboledwa Kuchoka Ku (1:1–18:27)**
   a. Mu Ukapolo (1:1–12:32)

1:1-7	5:1-23	9:8-17
1:8-14	6:1-13	9:18-35
1:15-22	6:14-30	10:1-20
2:1-14	7:1-7	10:21-29
2:15-25	7:8-13	11:1-10
3:1-9	7:14-25	12:1-13
3:10-22	8:1-15	12:14-22
4:1-13	8:16-32	12:23-32
4:14-31	9:1-7	

   b. Kuturuka / Kuchoka mu Ukapolo (Chiwombolo kudzera mu mwazi ndi mphamvu) (12:33–14:31)

12:33-41	13:1-16	14:1-12
12:42-51	13:17-22	14:13-31

   c. Ulendo wopita ku Sinai (Maphunziro) (15:1–18:27)

15:1-21	16:8-21	17:8-16
15:22-27	16:22-36	18:1-16
16:1-7	17:1-7	18:17-27

2. **Bvumbulutso lochokera kwa Mulungu (19:1–40:38)**
   a. Kuperekedwa kwa Malamulo khumi (19:1–24:18)

19:1-17	22:1-15	23:20-33
19:18-25	22:16-31	24:1-18
20:1-26	23:1-9	
21:1-36	23:10-19	

   b. Kukhazikitsidwa kwa Likasa (25:1–31:18)

25:1-9	26:31-37	29:31-46
25:10-22	27:1-8	30:1-21
25:23-30	27:9-21	30:22-33
25:31-40	28:1-43	30:34-38
26:1-14	29:1-9	31:1-11
26:15-30	29:10-30	31:12-18

   c. Kuphwanya kwa malamulo (32:1–34:35)

32:1-10	33:1-11	34:10-28
32:11-18	33:12-23	34:29-35
32:19-35	34:1-9	

   d. Kapangidwe ka likasa (35:1–40:38)

35:1-9	36:8-38	39:1-43
35:10-19	37:1-29	40:1-33
35:20-35	38:1-20	40:34-38
36:1-7	38:21-31	

Likasa la Yehova

(sichinajambulidwe motengera muyezo)



Levitiko

(Bukhu la Chiyero)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Mose ndiye Mlembi wa bukhuli. Dzina loti Livitiko limatanthauza kuti "zokhudzana ndi Alevi." Alevi anali alembi omwe anasankhidwa ndi Mulungu kuti azitumikira muuzimu pamtundu/pfuko lawo. Bukhu la Levitiko liri ndi malamulo ambiri omwe Mulungu anapereka kuti awongolere antu ndikutengera ku ntchito yolambira Mulungu.

Zaka: 1450–1410 B.C.

Mutu ndi Cholinga: Levitiko 14:45 amati ***"Mukhale oyera, pakuti Ine Yehova Mulungu wanu, ndine Oyera."*** Uphungu womwe unaperekedwa mu bukhu la Levitiko, ukusonyeza kuti Israeli anayenera kukhala oyera mtima pamaso pa Mulungu. Bukhu la Levitiko linapangidwa ndi cholinga chofuna kuphunzitsa mtundu wa a Israyeli zinthu izi: (1) momwe angakhalire komanso kuyenda ndi Mulungu; (2) Momwe Israyeli angakwaniritsire maitanidwe a Mulungu, monga dziko la unsembe. Mutu waukulu mu bukhu la Levitiko ndi chiyero kapena kuyera mtima **Kuziyeretsa** ndi njira yomwe imamupanga munthu kuti akhale oyera mtima, choncho, popeza Mulungu ndi woyera ndi opatulika; anthu amafika kwa Mulungu ndi nkhawa zawo kudzera mu ansembe monga ankhala pakati.

Anthu: Mose, Aaroni

Khristu mu Levitiko: Monga ku Eksodo, Khristu akupezekanso ndi kuchitiridwa umboni Mu Levitiko.

Zopereka Zisanu Zonsezi zikulongosol za umunthu ndi ntchito zones za Khristu mu moyo wake wopanda tchimo, ndi kuzipereka kwa Atate, ndi cholinga choti tikhale mu chiyanjano ndi Mulungu.

Ansembe a Akulu Amagwira ntchito yoimilira Khristu, mu bukhu la Levitiko.

Maphwando asanu ndi awiri Akulongosola za Mesiya, kutiphunzitsa za ungwiro wa munthu, kuzipereka nsembe kwake, kuukanso kwakufa, komanso dipo la ntchito yake yopambana.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Malamulo a Nsembe (1:1–17:16)**
   a. Kuti afikiridwe Mulungu (1:1–7:38)
      1:1-17 | 4:1-35 | 6:8-30
      2:1-16 | 5:1-19 | 7:1-38
      3:1-17 | 6:1-7
   b. Kwa ansembe (8:1–10:20)
      8:1-36 | 9:15-24
      9:1-14 | 10:1-20
   c. Zokhuza chiyero (11:1–15:33)
      11:1-12 | 13:1-59 | 15:1-33
      11:13-47 | 14:1-32
      12:1-8 | 14:33-57
   d. Zokhuzana ndi dipo la dziko (16:1–17:16)
      16:1-28 | 16:29-34 | 17:1-16

2. **Malamulo a Kudziyeretsa (18:1–27:34)**
   a. Pa anthu a Mulungu (18:1–20:27)
      18:1-30 | 19:9-37
      19:1-8 | 20:1-27
   b. Kwa ansembe a Mulungu (21:1–22:33)
      21:1-24 | 22:1-16 | 22:17-33
   c. Mu mapembezedwe (23:1–24:23)
      23:1-25 | 24:1-16
      23:26-44 | 24:17-23
   d. M'dziko la Kenani (25:1–26:46)
      25:1-22 | 25:35-46 | 26:1-13
      25:23-34 | 25:47-55 | 26:14-46
   e. Zokhudzana ndi malumbiro (27:1-34)
      27:1-13 | 27:14-34

Numeri

(Kuyendayenda mu Chipululu)

Mlembi ndi Mutu wa Bukhu: Bukhu la Numeri linalembedwa ndi Mose. Numeri amatanthauza "Chiwerengero." Dzina loti Numeri,linachokera ku Madera awiri a bukhuli: chaputala 1 ndi chaputala 26, momwe akulongosola za kuwerengera anthu a mtundu wa Israeli (Kalembera) Poyamba, paphiri la Sinayi, ndipo kachiwiri mu chigwa za Moabu.

Zaka: 1450–1410 B.C.

Mutu ndi Cholinga: Ngakhale Numeri anatenga dzinali kuchokera ku chiwerengero cha wanthu, komabe bukhuli lalongosola nkhani zones zomwe zinachitika mu zaka makumi anayi (40) momwe ana a Israeli anali pa ulendo wochoka ku Aigupto kupita ku Kenani. Ulendowu unayenera kuwatengera masiku khumi ndi mphambu ziwiri zokha (12), koma unawatengera zaka zochuruka zotere, zamazunzo mu njira monse, chifukwa cha kusakhulupilira komanso kugalukira kwa anthuwa.

Bukhu la Numeri, likutionetsera mavuto omwe amabwera ngati munthu alephera kuphatikiza chikhulupiliro pa malonjezano omwe Mulungu wapereka (Ahebri 3:16–4:2). Kuwonjezera apo, bukhu la Numeri limatiphunzitsa kuti; ngakhale moyo wa munthu umakhala ukukumana ndi zipululu za mavuto, koma sicholinga cha Mulungu kuti munthu apitilirebe kukhala mu mavutowa, kapena kufa ali mu zipsinjo zotere. Chisankho chomwe timapanga ndi chomwe chimatsogolera pa moyo wathu wa mtsogolo. Bukhu la Yoswa, litilongosolera bwino za nkhani ya chsankhoyi.

Mutu wina wofunika kwambiri mu bukhu la Numeri, ukupezeka pa chisamaliro chopanda malire cha Mulungu, kwa anthu ake nthawi ndi nthawi, mopanda kuwerengera mphulupulu, kusakhulupilika ndi kupanduka kwawo. Mulungu amapitilirabe kupereka zosowa za anthuwa kudzera mu zozizwa zosiyanasiyana. Mulungu anawapatsa iwo madzi, manna, ndi zinziri panthawi yomwe iwo anali kuzisowa ndi kugwira njakata. Mulungu anapitilirabe kuwakonda anthu ngakhale mu nthawi yomwe iwo amadandandaula. Amang'ung'uza, komanso amagalukira Yehova.

Anthu: Mose, Aaroni, Miriamu, Yoswa, Kalebu, Baraki

Khristu mu Bukhu la Numeri: Ngakhale palibe malo omwe malo oti Khristu analembedwa mu bukhuli, komabe, pali umboni wokwanira wa kupezeka kwa Khristu. Bukhu la Numeri likulosera za Khristu ndi kupachikidwa kwake pa mtanda, koposa kukwezedwa kwa chinjoka pa mtengo (Numeri 21:4-9; Yohane 3:14).

Thanthwe/Mwala lomwe panatumphuka madzi, anthu namwa ndikutha ludzu lawo, likuimilira Khrisu (1 Akorinto 10:4).

Mana omwe anagwa tsiku ndi tsiku aja akuimilira Khristu monga mkate wa moyo wochokera ku mwamba (1 Yohane 6:31-33).

Thambo ndi moto: Zikuimilira kuti Khristu ndiye wotsogolera, ndipo mizinda yobisalamoyo ikuimilira kuti Khristu ndiye pobisalapo pathu mu nthawi ya mavuto (Masalomo 50:15).

Ng'ombe ya msoti yofiira ikuimilira Khristu (Numeri 19).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Kukonzekera pa Sinai (Mbadwo wakale) (1:1–10:36)**
   a. Kuwerengera anthu/kalembera (1:1–4:49)

1:1-46	3:1-24	4:1-20
1:47-54	3:25-39	4:21-28
2:1-34	3:40-51	4:29-49

   b. Ungwiro wa Mulungu ndi kuziyeretsa kwa anthu (5:1–9:14)

5:1-10	6:22-27	8:5-22
5:11-31	7:1-89	8:23-26
6:1-21	8:1-4	9:1-14

   c. Ulendo wopita ku mdziko lolonjezedwalo (9:15–10:36)

9:15-23	10:1-10	10:11-36

2. **Kulephera/Kuperewera kwa Badwo wa Kale (11:1–25:18)**
   a. Kusakhutitsidwa kwa anthu adakali munjira (11:1–12:16)

11:1-9	11:16-30	12:1-16
11:10-15	11:31-35	

   b. Kupanda chikhulupiliro ku Kadesi-Bernea (13:1–14:45)

13:1-24	14:1-10	14:20-38
13:25-33	14:11-19	14:39-45

   c. Chilango chochokera kwa Mulungu (15:1–25:18)

15:1-13	18:8-32	21:21-35
15:14-31	19:1-22	22:1-21
15:32-41	20:1-7	22:22-41
16:1-40	20:8-22	23:1-30
16:41-50	20:23-29	24:1-25
17:1-13	21:1-5	25:1-9
18:1-7	21:6-20	25:10-18

3. **Kukonekera m'Badwo Watsopano (26:1–36:13)**
   a. Kukonzedwanso kwa Israeli (26:1–27:23)

26:1-65	27:1-14	27:15-23

   b. Malaulo a nsembe ndi malumbiro (28:1–30:16)

28:1-31	29:1-40	30:1-16

   c. Kugawa zigawo ndi malire a dziko (31:1–36:13)

31:1-24	32:1-42	33:50-56
31:25-54	33:1-49	

Deutoronomo
(Kubwerezanso Chilamulo)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: MleMbi wa bukhu la Deutoronomo ndi Mose. Mawu oti Deuteronomo ndi chingerezi chotanthauziridwa kuchokera ku mawu a abukhu a chiyankulo choya biliraa mu Baibulo ndipo akutanthauza "kuperekedwanso kwa chilamulo" ndipo anatengedwa pa Deuteronomo 17:18. Pa vesiyi antanthauzira molakwika poganizira kuti mlembiyi amatanthauza kuti bukhu linanso la malamulo achiwiri choncho, Deuteronomo sibukhu lachilamulo chinanso chachiwiri ayi, koma ndi bukhu lomwe labwerezanso kulongosola za chilamulo choyamba chomwe Mulungu anapereka paphiri la Sinai kudzera kwa Mose.

Zaka: 1410 B.C.

Mutu ndi Cholinga: ***Penyesetsani kuti mungaiwale***. Patapita zaka makumi anayi, ana a Israeli anali pafupi kulowa mu mzinda wolonjezedwa. Ndipo asanalowe mu nzindawo (Pofuna kuti asaiwale zones zomwe Mulungu anawachitira, kuchokera ku Aigupto, ndi munjira monse) iwo anakumbutsidwa za zones zomwe Mulungu anawacchitira, komanso za chilamulo chomwe chinali chofunika kwambiri, kuti athe kukhalamo bwino, mudziko la malonjezano ndi kugwira ntchito zones zoyenera monga mtundu woyeretsedwa, mtundu wosankhidwa ndi Mulungu, komanso monga ansembe achifumu ku maiko onse (Deutoronomo 4:1-18). Monga mbali imodzi yacholinga, bukhu la Deuteronomo likusindika pa kufunika kophunzitsa ana, za kumukonda ndi kumumvera Mulungu.

Bukhuli likuthera ndi nkhani ya kukonzedwanso kwa pangano la Mulungu kwa ana a Israeli (Mutu 29). Kudzera mu kusankhidwa kwa Yoswa kukhala mtsogoleri (Mutu 31), Mose atamwalira (Mutu 34).

Anthu: Mose, Yoswa

Khristu mu Bukhu la Deuteronomu: Pa mutu 18:15, Mose akulongosola momveka bwino za Khristu ndipo akuti ***"Yehova Mulungu Wanu Adzakuukitsirani Mneneri Pakati Panu, wa Abale anu Wonga Ine, Mumumvere Iye."*** Komanso Mose monga woimilira Khristu, anali yekhayo (kupatula Khristu) yemwe anakwanitsa maudindo onse atatu a mneneri: (34:10-12), Wansembe (Eksodo 32:31-35); komanso ntchito ya mfumu ngakhale iye sanali mfumu koma akugwira ntchito yolamulira Israeli, monga amachitira mfumu (33:4-5).[2]

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Malonje (1:1-5)**

2. **Kubwerezanso Mbiri (1:6–4:43)**

1:6-18	2:26-37	4:1-43
1:19-46	3:1-17	
2:1-25	3:18-29	

3. **Kubwerezanso/Kuwonanso Chilamulo (4:44–5:33)**

4:44-49	5:1-21	5:22-33

4. **Kugwiritsa Ntchito Chilamulo (6:1–11:32)**

6:1-25	9:1-29	11:1-32
7:1-26	10:1-11	
8:1-20	10:12-22	

5. **Malaulo Ena Owonjezera (12:1–26:19)**

12:1-32	18:9-22	23:1-25
13:1-18	19:1-13	24:1-5
14:1-29	19:14-21	24:6-22
15:1-23	20:1-20	25:1-19
16:1-22	21:1-23	26:1-19
17:1-20	22:1-12	
18:1-8	22:13-20	

6. Kulandira Pangano (27:1–30:20)

27:1-26	28:15-68	30:1-14
28:1-14	29:1-29	30:15-20

7. Kusintha Mtsogoleri (31:1–34:12)

31:1-13	32:1-52	34:1-12
31:14-30	33:1-29	

Phunziro Lonse wa Mwachidule

Genesis	Kusankhidwa kwa mtundu wonse
Eksodo	Kuwomboledwa kwa mtundu wa anthu
Levitiko	Kuyeretsedwa kwa mtundu wa anthu
Numeri	Kuwongoleredwa kwa mtundu wa anthu
Deuteronomu	Kuphunzitsidwa kwa mtundu wa anthu

Gawo 2
Mabukhu a Mbiri

Ndime zosiyana za Chipangano Chakale zikulongosola mwa chindunji za Umunthu wa Khristu. Kuyambira bukhu la Yoswa mpaka Estere, tikakhala tikuwona gulu lachiwiri la mabukhu am'Baibulo lomwe limakamba za mbili (nthano) fuko la Israel. Mabukhuwa akufotokoza za moyo wonse wa pfko la Israel kuchokera pamene anafika ku dziko lawo lamalonjezano mpaka nthawi ziwili zomwe anagonjetsedwa, nalandidwa ulamulilo chifukwa chakusakhulipilira ndi kusamvera Mulungu. Mabukhuwa akufotokoza zomwe zinachitika kwa zaka mazana asanu ndi atatu (800) ku mtudu wa Israel. Zina mwa izo zinali kugotsetsedwa ndi kutengedwa kwa kenani, ulamulilo wa oweruza, kukhazakitsidwa kwa ulamulilo wa mafumu, kugawidwa kwa Israyeli kukhala zigawo ziwili: Ufumu wakumpoto ndi ufumu wakumwera, kutha kwa kumpoto utagonjetseredwa ndi Assuri, kutengedwa ukapolo kwa ufumu wa kum'mwera mu Baibulo, komanso kubwereranso kwa pfukoli kupita Yerusalemu pansi pa utsogoleri wa Nehemiya ndi Ezara.

Popeza mabukhuwa akulondolera ndi kukonzekeretsa zakubwera kwa Khristu, mesiya, choncho mabukhuwa akufotokoza motere:

Mabukhu a Mbiri Kukonzekera Khristu[3]		
Yoswa Oweruza Rute	Kulandila umwini wa malo Udziko la malonjezana Komanso kuphinjidwa kwa pfuko	Ulamuliro wa Mulungu: Mabukhu atatu awa akulongosola za nthawi yomwe dziko la Israyeli limalamulidwa ndi Mulungu (1405–1043 B.C.)
1 Samueli 2 Samueli 1 Mafumu 1-10 1 Mafumu 11-22 2 Mafumu 1-17 2 Mafumu 18-25 1 Mbili 2 Mbili	Kukhazikika kwa pfuko la Israel Kukula kwa pfuko Kudaliisika kwa pfuko Kugawikana kwa pfuko Kutha /kolowa pansika ufumu wakumoto Kusamukira ku ufumu wakumpoto Kumanga Kachisi Kuonongeka kwa Kachisi	Dziko lolamulidwa ndi mafumu: Mabuku awa akulongosola Mabukuatane awa akulongosola tsatanetsatane wa mbili ya ufumu wa Israyeli kuchokera nthawiyomwe pfuko lina inakhazikitsidwa ngati dziko kufikira pa nthawi yomwe linawonongedwa (586 B.C.).
Ezekile Nehenya Estere	Kukodzedwa kwa Kachisi Kukodzedwa kwa Yerusalemu Chitetezo pa anthu a pfuko la Israel	Kubwezeretsa: Mabukhu atatuwa akulongosola za kubweratso kwa pfuko la Israel kudziko lawo zaka (zaka 70) mazana asanu ndi awiri kumpoto (605–535 B.C.).

Yoswa
(Umwini ndi Chigonjetso)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Mlembi wa bukhuli ndi Yoswa, mosiyana ndi mabukhu asanu oyambirira m'Chipangano Chakale aja bukhu layoswa likutenga dzina lake kuchokera pa mlembi wake Yoswa, mtumiki wa Mose. Dzina lake lenileni la Yoswa linari Hoseya (Numeri 13:8; Deutoronomo 32:44) mwana wanuni, wa pfuko la Efremu. Mawu oti Hoseya akutanthauza "chipulumutso," koma munthawi yomwe ana a israer anari kuyenda muzipululu pa alendo wawo wopita ku dziko la malonjezano mose anasintha dzina la Hoseya kukhara yehoshua, kutanthauza kuti "Yahweh ndiye chipulumutso" (Numeri 13:16) ndipo pakupita kwa nthawi dzina la Yoswa linabadwa kuchokera pa dzina la Yehoshua dzina loti Yahweh ndiye chipulumutso linari chowakumbutsa ana a israel, Yoswa mwini, komanso azondi kuti chigonjetso chiri mmanja mwa Yehova osati mu mphamvu ndi malingariro a munthu ayi bukhuri linapatsidwa dzina limeneri chifukwa ngakhare Yoswa anali mmodzi wa asirikali ozama mu mbiri ya pfuko la Israel, nzeru za ke komanso chipambano mu usilikari wake zinachokera kwa Mulungu yemwe payekha ndiye chipulumutso chathu. Anali Mulungu yekha yemwe anapansitsa kuti pfuko la Israyeli ligonjetsedwe ndi kupambana adani ake onse ndikulandila dziko lawola malonjezano.

Zaka: 1400-1370 B.C.

Mutu ndi Cholinga: Umwini, chigonjetso ndi kugawidwa kwa dziko la malonjezano ndicho cholinga ndi mutu wa nkhani Bukhu la Yoswa linalembedwa mwaukadaulo pofuna kutsimikiza za kukhulupiliaka ndi kusazengereza kwa Mulungu pa malonjezano ake kwa anthu Mulungu anachita monga momwe analonjezera (Genesis 15:18; Yoswa 1:2-6; 21:43-45). Nkhani zonse zomwe zalembedwa mu bukhu la Yoswa ndizosankhika zolongosola bwino za m'mene Mulungu amalowererapo ndi kuthandiza kugonjetsa adani mwa anthu ake Mulungu anakwanitsa malonjezano ake onse omwe anena kwa Abraham ndi Sara okalambawo, mpaka nthawi

yomwe pfukololi linalandila umwini wadziko lawo la malonjezano ndi mizinda yake, dziko loyenda mkaka ndi uchi. Iyi ndiyo ntchito ya Mulungu, ntchito yomwe munthu sangayikwanitse ngakhale atayesera motani mu mphamvu ndi malingaliro ake a kuthupi (Aroma 4).

Anthu: Yoswa, Rahabu, Kalebu

Khristu mu Nkhaniyi: Ngakhale bukhuli silikutchula dzina la Khristu mumauneneri ake okhudza Mesiya, tikuwona kuti ali mbali ziwiri zomwe zikulongosola za mpulumtsi Yoswa ndi chizindikiro cha Khristu mu mfundo ziwiri zofunikitsitsa. Choyamba YESHUA chidule cha dzina Yehoshua, kutathauza kuti "YAHWEH ndiye chipulumutso" ndi mawu a chiHelene (Greek) likutchulidwa kuti Yesu mu matchitidwe 7:45. Chachiwili Yoswa akuwoneka ngati Khristu kudzera mu ntchito yake yotsogolera Israel ndi mfumu ya chimwemwe polowa mu dziko la "mpumulo," dziko la malonjezano, dziko la kenani (Ahebri 4:8). Uwu ndi "mpumulo" tinaulowa mwa chikhulupiliro wopezeka kwa Yesu Khristu. Choncho Yoswa akuprreka chithunzithunzi ndi ulosi wa mpulumutsiyemwe adzasogolera "Ana ake ambili ku ulemelero" (Ahebri 2:9-10). Yoswa anakumana ndi kazembe wa ankhondo Yehova (Yoswa 5:13-15) ndipo ichi ndi chosakaikitsa kuti ziikuimilira kuonekera Khristu mwa umulungu (komwe kumatchedwanso chritophany) emwe anafika kuzamuphunzitsa Yoswa kuti iye si msilikali wamba ayi koma kazembe wa akhondo. Potsiriza, chingwe chofila cha Rahabi chikuimila chipulumutso kudzera mu mwanzi wa Yesu Khristu (Ahebri 9:19-22). Mzimayi wadama wachikinja (Rahabi) anamva za ntchito zoziwika za Mulungu, nayamba kukhulupilira anahandiza kubisa azondi, ndipo pachifukwa ichi, Rahabi anapulumuka, naombola pamene mzinda wa Yeriko unawonongeka ndipo Rahab anapezeka mu Baibulo pa ndandanda wa makolo a Yesu Khristu (Mateyu 1:5).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Kulowa mu Kenani (1:1–5:12)**

1:1-9	2:1-24	4:1-24
1:10-18	3:1-17	5:1-12

2. **Chigonjetsa cha Kenani (5:13–12:24)**

5:13-15	8:135	10:29-43
6:1-27	9:1-27	11:1-23
7:1-15	10:1-15	12:1-24
7:16-26	10:16-28	

3. **Kugawidwa kwa Kenani (13:1–21:45)**

13:1-33	17:1-18	20:1-9
14:1-15	18:1-10	21:1-45
15:1-63	18:11-28	
16:1-10	19:1-51	

4. **Mathero a Nkhani (22:1–24:33)**

22:1-34	24:1-28
23:1-16	24:29-33

Oweruza

(Zachipasuko, Chiweruzo ndi Chiwombolo)

Mulembi ndi Dzina la Bukhu: Mphekesera zimati mulembe wa bukhu la Oweruza ndi Samueli koma palibe umboni otsimikiza izi. Samueli mwina amangosanja mwa dongosolo nkhani zonse zochokera mu nkhani ulamuliro wa Oweruza, koma zikusonyeza kuti Natani ndi Gadi ndi amene anagwira nchito yosandula ndi kufotokoza bwino za bukhuli (1 Mbiri 29:29).

Mawu oti oweruza mu chi Hebri ndi Shophetim kumasulira kuti "olamulira, owombola, opulumutsa." Mawu oti Shophetim sason yeza izi zonkha ayi–mawuwa akunthndawuzanso kuti kuyanjanitsa ndi kuwombola anthu pa mabvuto. Poyamba oweluza amawombola anthu ndipo atatelo analamulira ndi kuyang'anila komanso kulongosola ntchito za chilungamo.[4]

Dzina la bukhuli [Oweruza] linabwera chifukwa pa nthawiyo dziko ndi mfuko la Israyeli linayendetsedwa ndi utsogoleri wa Oweruza, ndipo Oweruza anawombola Israyeli m'manja mwa opondereza. Mutu bukhuli ukulongosola bwino (pa Oweruza 2:16) ***"ndipo Yehova anawutsa Oweruza kuti awapulumutse ana a Israyeli m'dzanja lawo akuwafunkha (akuwapondereza)."*** Zowona zake ndi zakuti Mulungu ndi amen anali mumuomboli chifukwa ndiamene analoleza nyengo yakuumboledwa kwa ana a Israyeli kuti iwafikile ndicholinga

chofuna kuwaphuzitsa makhalidwe abwino auzimu, popeza Israel ankapitilizabe kuchita zoipa ndi kusakhulupirila, ndipo Mulungu anawutsa Oweruza kuti abweretse chiwombolo ku Israyeli pamene iwo anabvomereza kulakwa kwawo. Ndipo iwo analira nalapa kwa Mulungu kuti awanthandidze (Oweruza 11:27; 8:23).

Zaka: 1050–1000 B.C.

Mutu ndi Zochitika: Kusiyana kwapakati pa bukhu la Yoswa ndi oweruza ndikoti bunkhu la oweruza likunena za kusintha kwa ana Israel kuchoka mu chigonjetso ndikulowa muzisoni, ziphinjo, mavuto ndi kugonjetsedwa. Kuchoka mu ufulu kupita muukapolo ndikuponderezedwa. Kuchoka mukupambana analinako kupita ndikufika mukulephela.

Kufotokezera monga mwambiri: Oweruza akubweretsa pamodzi kapena kulumikiza pakati pa nkhawi ya Yoswa nthawi ya mneneri Samueli ndikuyambika kwa maufumu mu Israyeli pansi paulamuliro wa Davide, Bunkhu la oweruza linalemba mbiri ya kuzilala kwa oponderezedwa. Pemphero ndi kuwomboledwatso kwa pfukoli ndipo pakutero likulongosolanso chifukwa panali pofunika kwa pfukoli kuti likhale ndi maufumu. Popeza aliyese ankagochita chomwe akufuna, panali pofunikiladi kwambiri kuti pakhale mtsogoleri wa mfumu yolungama pakati pawo (Oweruza 21:25).

Kufotokozera monga mwachiphunzitso: Oweruza akufotokozera ife kuti za choonadi chofunikira kwambiri. Monga momwe Mulungu anachenjezera mubukhu la Deuteronomo, kumvera kunabala mdalitso, ndipo kusamvera munabala chilango, mkwiyo wa Mulungu ndi kupondereza. Oweruza amatikumbusaso kuti anthu akabweranso kwa Mulungu, nalila mofuula kwa iye, nalapa zoipa zawo; Mulungu yemwe ndi opilira wa zisomo komanso wokhululuka, adzayankha ndikuombola anthuwo. Bukhu la Oweruza likutambatsula kwambili za nyengo zingapo zomwe anthu anapanduka kwa Mulungu natsata njila zao zoipa, zotsatira zake iwo anagonjetsedwa, naponderezedwa, chifukwa Mulungu anakwiya napereka chilango kuti aphunzire ndi kuleka njira zawo zoipa. Pamapeto pake anthuwa analapa, ndipo Mulungu anawutsa Oweruza kuti awombole pfuko.

Anthu: Othnieli, Ehudu, Samaga, Dedorah, Balaki, Gidioni, Tola, Yaire, Yafuta, Ibizani, Eloni, Abadoni ndi Samson. Oweruza ome amadziwika bwino anali Deborah, Gidioni ndi Samson.

Khristu mu Bukhu la Oweruza: Popeza oweruza aliyese ankagwira ntchitoyi ngati wolamulira, woombola, izi zikupeka chithunzithunzi cha mpulumutsi ndi ntchito yake monga mpulumutsi ndi Ambuye, mfumu yachilungamo yoombola anthu.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Kugwa–Ciyambi: Chifukwa Chakufunika kwa Oweruza (1:1–3:8)**

1:1-26	2:1-5	2:11-23
1:27-36	2:6-10	3:1-8

2. **Kuwomboledwa–Mbili ndi Ulamuliro pa Nthawi ya Oweruza (3:9–16:31)**

3:9-14	7:19-25	12:8-10
3:15-30	8:1-27	12:11-12
3:31	8:28-35	12:13-15
4:1-24	9:1-22	13:1-25
5:1-31	9:23-57	14:1-11
6:1-8	10:1-2	14:12-20
6:9-27	10:3-18	15:1-20
6:28-35	11:1-28	16:1-17
6:36-40	11:29-40	16:18-27
7:1-18	12:1-7	16:28-31

3. **Tchimo–Kuchita za Chisawawa ndi Kupasuka. Kugonjetsedwa pa Nthawiya Ulamuliro wa Oweruza (17:1–21:25)**

17:1-13	20:1-17	21:8-25
18:1-31	20:18-48	
19:1-30	21:1-7	

Rute
(Choonjezera pa Bukhu la Oweruza)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Monganso bukhu la Oweruza, mlembi wa bukhu la Rute sakudziwika, ngakhale mbili ya Chiyuda imati mlembi wa Rute anali Samueli. Bukhuli linatenga dzina lake kchokera kwa Rute yemwe anali mwini khani mu bukhuli. Rute anali mtsikana wa ku Moabu, chidzukulutudzi cha Davide yemwe alinso pa mdandanda wa makolo a mpulumutsi (Yesu) (Mateyu 1:5). Bukhu lina m'Baibulo lomwe linatchulidwa dzina la mzimayi ndi Estere.

Zaka: 1050 B.C.

Mutu ndi Cholinga: Bukhu la Rute likufotokoza za nthano ya banja lina la mu Israyeli, lomwe nthawi ina kuli chilala, anasamukila ku Moabu kuti akapeze zakudya ndikupulumuka ku njala. Ndipo ali kuMoabu, mwamuna ndi ana ake awiri anamwalira nasiya mayi (Naomi) ndi ake aakazi awiri (Olipa ndi Rute). Choncho, Naomi anaganiza zobwerera kwawo ku Israeli ndipo Rute anaumila kupita limodzi ndi apongozi ake (Naomi). Ndipo atafika ku Israel, iwo anapita kwa m'bale wawo dzina lake Boazi: kumapeto kwake Boazi anadzakwatiranso Rute.

Monga mwala wonyezimila, Rute anawala kopambana mthawi ya mdima imeneyi, nthawiyi ya ulamuliro wa Oweruza. Bukhu la Rute ndi nkhani ndi nkhani ya kukhulupilika, kuyera mtima ndi chkondi pa nyengo ya chisawawa, nyengo ya mavuto, nyengo yosowa mtsogoleri. Kudzikonda ndi kuponderezana ndilo linali khalidwe la nthawi, koma ngakhale zinali chotero, Rute sachita mkhalidwe oipawu koma iye amapereka chitsanzo chabwino cha chikhulupiliro ndi kumvera ngakhale inali nthawi yovuta ya chipasupasu ndipo chifukwa cha chikhulupiliro chake, Rute analandila madalitso. Rute akufotokodzeredwanso monga mzimayi wa pfuko la Davide mu ndandanda wa makolo a Yesu (Messiah) (Mateyu 1:1-5). Mubukhu la Rute tikupezamonso choonadi cha muthu woombola, kupezeka kwa anthu opulumuka ngakhale munyengo ya chipasupasu ndipo tikuwonanso za kukhulupilika kwa Mulungu pa anthu omwe amayenda ndi kukha la mwa iyemwa chikhulupiliro. Popeza Rute analiwamitundu (osati wa pfuko la Israel) bukhu la Rute likutionetsa kuti Mulungu ali ndi chifuniro chabwino kwa anthu amitundu kuti akhale ana am'banja lake losankhidwa.

Zimawoneka ngati zodabwitsa kuona kuti munthu yemwe amakonda Mulungu mopanda chinyengoyu anali wa pfuko la Moabu, koma chifukwa cha kukhulupirika kwake kwa Mulungu ndi ku banja la Israyeli lomwe iye anadzakwatiwako kale, ndi kukakamila kwake kukhalabe ndi mpongozi wake Naomi mpakana kusamuka naye limodzi kupita ku Israel Naomi akuwengedwa monga mwa na wa mkazi weni weni wa pfuko la Israyeli, wokwanila kutchulidwa mbumba ya Davide. Apa zikutiphunzitsa kuti kulowa mu ufumu wa Mulungu kumachitika kudzera mu chisankho ndi chivomerezo chomwe munthu wachipanga osati kudzera mu pfuko (mtundu), magazi kapena dziko akuchokera ayi, koma kudzera mukukhupilira ndi chikhulupiliro (Aroma 1:5). Kupezeka kwa Rute mu mbumba ya Davide, kukutiphunzitsa kuti mu ufumu wa mwana wa Davide (Yesu) mudzakhala anthu a mitundu yonse ya pa dziko lapansi mopanda tsakho.[5]

Anthu: Rute, Nomi, Boazi

Khristu mu Nkhaniyi: Muchipangano cha kale, ngati munthu kapena katudu anagultsidwa, amatha kuwomboledwa kudzera mundondommeko yotchedwa chiwomblo cha mwamuna. Mu chihebri, momboli amatchedwa "GOEL" kutanthauza mnasi (m'bale). Ndondomeko yotere ikupezeka chitsanzo cha ntchito ya mpulumutsi.

GOEL (m'bale) amayenera kukhala wobadwa naye bele limodzo, ndipo iye ndiyemwe amawombola (Deutronomu 25:5, 7:10; Yohane 1:14; Aroma 1:3; Afilipi 2:5-8; Ahebri 2:14-15). M'baleyu amapereka dipo la chiwombolo mwa mtengo wake wotchulidwaw (Rute 2:1; 1 Petro 1:18-19). Mbaleyu anayenera kukhala munhu yemwe akufunitsitsa kupereka chiwombolo (Rute 3:11; Matyu 20:28; Yohane 10:15, 19; Ahebri 10:7). M'baleyu amayenera kukhara mfulu iye mwini, monga Khristu anali mfulu, wopanda tchimo kapena tembelero, wolungama (1 Akorinto 5:21; 1 Petro 2:22; 1 Yohane 3:5).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Chisankho ndi Kubwera kwa Rute (1:1-22)**
   1:1-5 1:6-18 1:19-22

2. **Ufumu Rute (2:1-23)**
   2:1-3 2:4-17 2:18-23

3. **Pempho la Rute (3:1-18)**
   3:1-4 3:5-9 3:10-18

4. **Mphoto ya kukhulupilika kwa Rute (4:1-22)**
   4:1-12 4:13-17 4:18-22

1 Samueli

(Kusintha kwa Ulamuliro ku Pfuko la Israyeli Kuchokera kwa Oweruza Kupita kwa Mafumu)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Mlembi wa bukhu la 1 ndi 2 Samueli sakudziwika bwinobwino. Mbiri yochokera kuchiyuda imalongosola kuti mabukhu awiriwa anali Samueli. Ngakhale mabukhu awiriwa, 1 ndi 2 Samueli analembera anapatsidwa dzina la Samueli mneneriyo. Sizikanatheka kuti Mneneriyo kuti alembe theka la bukhu loyamba la 1 Samueli chifukwa m'bukhu lomweli pa chaputala cha 25, mwalembedwa za 10:25 tikumva kuti Samueli ndiye mlembi wa bukhuli. Komanso bukhu la 29:29 ikufotokoza mwachimvekere kuti Gadi ndi Natani ndi anthu omwe analemba zochitika za m'mabukhu a Samueli.

Pachiyambi, mubukhu a Sumuel 1 ndi 2 anali bukhu limodzi m'chiyankhulo cha chi Hebri. Mabukhuwa analongosola bwino mbiri ya maufumu a pfuko la Israeli kuchokera kumayambiliro a ufumu. Bukhu la 1 Samueli ndi bukhu la 2 Samueli likulongosola za mfumu Davide.

Choncho, ngakhale mabukhuwa anali bukhu limodzi pachiyambi, anthu omwe anatanthauzira malembawa kuchokera ku mpukutu wa bukhu lopatulika wa kale wa muchiyankhulo cha chihelene (Greek). Kugawidwa mabukhuwa kunatsatiridwanso ndi Jerome mu chiyankhulo cha Latini, kenako kufikira ziyankhulo zina zonsezi.

Zaka: 1010 B.C.

Mutu ndi Cholinga: Kuyambira ndi kubadwa kwa Samueli ndi kuphunzira kwake mu Kachisi, 1 Samueli amafotokoza momwe mtumiki uyu wa Mulungu anatsogolera pfuko la Israyeli monga M'neneri, Wansembe, komanso ngato Oweruza wotsiriza (chitseka khomo). Munthawi yomwe Sameul anali kulamulira, mtundu wa Israeil, pamene iwo amafunisits a kuti azikhala monga dziko osati pfuko chabe, anawonetsa kuti iwo akufuna kukhala ndi mfumu woti aziwatsogolera. Kudzera mu mphamvu ya Mulungu, Samueli anadzodza Sauli kukhala mfumu ya dzikoli, Koma Sauli anakanidwa ndi Mulungu chifukwa cha kusamvera kwake, ndipo sanapitilire kulamulira. Potsatiranso mphamvu ndi chisankho cha Mulungu, Samueli Davide, munthu wa pamtima pake pa Mulungu, yemwe Mulungu mwini anamusankha kuti akhale Mfumu ya Israel. Nkhani zotsatira, zikulongosola za nkhani zomwe zinachitika chifukwa cha nsanje yomwe Sauli anali nayo kwa Davide woopa Mulunguyo.

1 Samueli akupitirizabe kulongosola za mbiri ya Israyeli kuchokera pomwe Oweruza anatsirizira kulamulira, ndipo chitsirizira cha Oweruza chinali Samueli, yemwe analamulira utatha ulamuliro wa Samson (Oweruza 16:31). Bukhu ili limalondoloza za kusinthika kwa ulamuliro wa Israel kuchokera kwa oweruza kufika pa Mafumu, kuchokera ku ulamuliro wa oweruza kufika ulamuliro wa chifumu. Munyengo yomwe oweruza amalamulira, mtundu wa Israel sumalore kuki alamulire miyoyo yawo. Wina aliyense anali kuchita chomwe iye amachiona kuti chikumukomera (Oweruza 17:6; 21:25). Ulamuliro wa mafumu unabweretsa kukhazikika komanso kusunga mwambo, chifukwa anthu anali ofunitsitsa kumvera ndi kukhala pansi pa ulamuliro wa mfumu ya padziko lapansi. Munthu wooneka ndi maso. Mulungu anamuuza Samueli ***"umvere mawu awo onse ali kulankhula nawe anthuwo, popeza sanakukane iwe, iwowo anakana ine kuti ndisakhale mfumu yawo"*** (1 Samueli 8:7).

Mulungu anafunisitsa kuti apereke mfumu ku mtundu wa Israel (Genesis 49:10; Deutronomu 17:14-20), koma anthu anakana kudikira kuti Mulungu awapanse mfumu, mmalo mwake iwowo anadzisankhira okha mfumu ya kumtima kwawo. Mulungu anakana Sauli chifukwa iye anakana kutsatira mawu akuti ***"kumvera kuposa nsembe yopsereza…*** (1 Samueli 15:22). Sauli asasanduka wa khalidwe la nsanje, wopusa, wokhumudwitsa komanso wachimasomaso. Koma Mfumu Davide anasonyeza ndikutipatsa phunziro kuti ***"Mulungu sauna monga munthu owonera, Munthu amayang'ana chooneka pa maso, Yehova amayang'ana mumtima"*** (1 Samueli 16:7). Mulungu anakhazikitsa ufumu wa Davide chifukwa cha kumvera kwake Davide, nzeru zake komanso moyo wake wodalira pa Mulungu.[6]

Cholinga chenicheni cha bukhu la 1 Samueli ndi chofuna kulemba chiyambi chake cha ufumu wa Davide woopa Mulungu.

Anthu mu Nkhaniyi: Mneneri Samueli, Sauli mfumu yosamvera, Davide mbusa woweta nkhosa.

Khristu mu Bukhu la 1 Samueli: Samueli akutipatsa chithunzi cha kupezeka kwa Khristu mwanjira yonena kuti iyeyu anali Mneneri, wansembe ngakhale iye sanali mfumu koma anali woweruza yemwe Mulungu anamugwiritsa ntchito kuti akhale wolamulira mpaka chomwe Israeli anayamba kulamulira dzikoli.

Mesiya akutanthauza "wozozedwa," ndipo Samueli ndi bukhu loyamba la mu Baibulo kutchula mawu oti "wozozedwa" (1 Samueli 2:10). Mesiah akulongosoledwa mu kudzera mu moyo wa Davide. Iye anabadwira ku Betelehemu, anagwira ntchito monga mbusa woweta nkhosa, anakhhalanso mfumu wolamulira ndiponso anakhala kholo pa mbadwo wa Mesiya Mfumu ya mafumu kudzera mu ufumu wake (Davide). Ku chipangano chatsopano, Khristu amamasuliridwa ndi kutculidwa kuti ***"mphukira*** (mbewu) ***ya Davide monga mwa thupi"*** (Aroma 1:3).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Samueli, Oweruza Wotsiriza (1:1–8:22)**
   a. Kuitanidwa kwa Samueli ndi Mulungu (1:1–3:21)
   1:1-18 2:12-17 3:1-21
   1:19-28 2:18-21
   2:1-11 2:22-36
   b. Ntchito ndi Utumiki wa Samueli (4:1–7:17)
   4:1-22 6:1-21
   5:1-12 7:1-17
   c. Kukhuzika/kusweka mtima kwa Samueli (8:1-22)
   8:1-9 8:10-22

2. **Sauli, Mfumu Yoyamba ya Israeli (9:1–15:35)**
   a. Kusankhidwa kwa Sauli ndi anthu (9:1–12:25)
   9:1-14 10:17-27 12:12-25
   9:15-27 11:1-15
   10:1-16 12:1-11
   b. Kukanidwa kwa Sauli (13:1–15:35)
   13:1-23 14:24-46 15:1-9
   14:1-23 14:47-52 15:10-35

3. **Davide, Mfumu Yotsatira (16:1–19:24)**
   a. Davide, Mbusayo, wosankhidwa komanso wozozedwa (16:1-23)
   16:1-11 16:12-23
   b. Davide, Wakuphayo, atsatidwa tsatidwa ndi Sauli (17:1-58)
   17:1-19 17:20-30 17:31-58
   c. Davide, mzake wa Yonatan, Koma Akanidwa ndi Sauli (18:1–19:24)
   18:1-9 18:20-30
   18:10-19 19:1-24

4. **Davide, Asocheretsedwa ndi Sauli (20:1–26:25)**
   a. Davide atetezedwa ndi Yonatani (20:1-42)
   20:1-29 20:30-42
   b. Davide atetezedwa ndi Ahimeleki (21:1-9)
   c. Davide atetezedwa ndi Akisi (21:10-15)
   d. Davide ndi gulu la Amuna (22:1–26:25)
   22:1-23 24:1-22 25:18-38
   23:1-14 25:1 25:39-44
   23:15-29 25:2-17 26:1-25

5. **Kubisala kwa Davide mu Dziko la Afilisiti (27:1–31:13)**
   a. Davide akhala kapolo wa Afilisiti (27:1–28:2)
   b. Sauli apita kwa asing'anga ndi owombeza (28:3-25)
   c. Davide amasulidwa ndi Afilisiti (29:1-11)
   d. Davide akatha Aa maleki (30:1-31)
   e. Afilisiti, ndi imfa ya Afilisiti (31:1-13)

2 Samueli

(Ufumu wa Davide–Kukula kwa Pfuko)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Popeza mabukhu a 1 ndi 2 Samueli linali bukhu limodzi pachiyabi asanagawidwe pawiri nkhani ya mlembi ndi dzina la bukhuli takamba kale kuti mu 1 Samueli.

Zaka: 1010 B.C. (komanso mtsogolo)

Mutu ndi Cholinga: Bukhu la 2 Samueli likupitirizanso kufotokoza za kuyamba kwa ufumu wa Israeli kuyambira pa imfa ya Mfumu Sauli mpaka ulamuliro wa Davide. Davide analamulira kwa zaka 40 (makumi anayi) (2 Samueli 5:4-5) ndipo imafufuzanso ndi kuunikira za zipambano ndi zipsinjo za mfumu Sauli, zomwe zina mwa izo ndi tchimo lake la chigololo, tchimo la kupha, ndi zipsinjo zina ku banja lake ndi ku dziko lake. Mutu weniweni wa 2 Samueli womwe ukunena za ufumu wa Davide unayenera kukhala "momwe tchimo limasinthira chimwemwe kukhala mavuto." Ndipo ufumu womwe unayambika ndi mfumu Sauli, unapitirira kukuzidwa ndi Davide mfumuyo. Ufumu wa Sauli unapereka kukhazikika kwa Israeli kuchokera munthawi ya ulamuliro wa oweruza koa Daide atakhala mfumu, Israeli anakula ndi kutambasuka. Ndipo bukhu la 2 Samueli likulongosola bwino nkhani zabwino ndi zoipa za moyo wa Davide.

Anthu: Davide, Baseba, Natani, Abisalomu, Aminoni, Aiyitopeli

Khristu mu Bukhu la 2 Samueli: Kupatulapo machismo ake, Davide anakhalabe chitsanzo cha Khristu mu ufumu wa Israeli ndipo Mulungu anakhazikitsa pangano kwa Davide lomwe liri ndi chikwaniritso cha umunthu wa Khristu.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Zikondweretso za Davide (1:1–10:19)**
   a. Davide azozedwa ufumu (1:1–5:5)

1:1-16	2:12-32	3:31-39
1:17-27	3:1-5	4:1-12
2:1-7	3:6-25	5:1-5
2:8-11	3:26-30	

   b. Cholimbikitsa mtima/chokondweretsa Davide (5:6–6:23)

5:6-25	6:1-11	6:12-23

   c. Pangano lokhudzana ndi ufumu (7:1-29)

7:1-7	7:8-17	7:18-29

   d. Kugonjetsedwa kwa mfumu (8:1–10:19)

8:1-18	9:1-13	10:1-19

2. **Tchimo la Mfumu (11:1-27)**
   a. Mfumu ichita tchimo la chigololo (11:1-13)
   b. Mfumu ikonza chiwembu chakupha munthu (11:14-27)

3. **Mavuto la Mfumu (12:1–24:25)**
   a. Mavuto kunyumba kwa mfumu (12:1–13:36)

12:1-14	12:24-25	13:1-23
12:15-23	12:26-31	13:24-36

   b. Mavuto mu ufumu wake (13:37–24:25)

13:37-39	17:1-14	20:13-26
14:1-20	17:15-29	21:1-22
14:21-33	18:1-18	22:1-51
15:1-12	18:19-33	23:1-7
15:13-37	19:1-7	23:8-39
16:1-4	19:8-43	24:1-14
16:5-14	20:1-9	24:15-17
16:15-23	20:10-12	24:18-25

1 Mafumu

(Imfa ya Mfumu Davide–Kusokonezeka kwa Ufumu)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Mlembi wa bukhuli sakudziwika, ngakhale aYuda amanena kuti bukhuli linalembedwa ndi Yeremiya. Koma Dr. Charles Ryrie analongosola za mlembi wa bukhuli motere:

> Ngakhale yemwe analemba kapena kusanja bukhu la mafumu sakudziwika, koma poddzindikira kuti munthuyo anagwiritsa ntchito nthano za (11:41; 14:19, 29); choncho, mlembiyo ayenera kuti anali mmodzi mwa ana a Israeli omwe anagwidwa ukapolo ku Baibulo. Sakudziwika mlembi weniweni, mwina anali Ezara, mwina Ezekieli, kapena Yeremiya, koma pozindikira kuti Yeremiya anamwalira ku Aigupto, osati ku Baibulo, choncho mlembi wa chaputala chotsiriza cha Mafumu ayenera kuti anali munthu wina.[7]

1 ndi 2 Mafumu, poyamba linali bukhu limodzi (monganso 1 ndi 2 Samueli komanso 1 ndi 2 Mbiri) ndipo mwachidule bukhuli limatchulidwa Mafumu, mu chihebri amati (Melechim), popeza amafufuza mbiri ya Israeli ndi Yuda pa nthawi ya ulamuliro wa Solomoni mu ukapolo wa ku Babulo. Bukhu la 1 Mafumu ikutha ndi nkhani ya ulamuliro wa mfumu wa Ahaziah mu 853 B.C.

Zaka: 550 B.C. Kumasulidwa kwa Yehoakimu kuchokera ku ndende ndiyo nkhani yomalizira ya bukhu la 2 Mafumu. Nkhani imeneyi inachitika mu zaka 37 za kumangidwa kkwake mundende (560 B.C.) Choncho,1 ndi 2 Mafumu analembedwa zitapita izi. Ndipo zikuoneka kuti kuchoka kwa Israyeli ku Baibulo mu chaka cha 516 B.C. sinali nthawi yomwe 1 ndi 2 Mafumu analembedwa. Zikanakhala kuti zinali motero, mlembi wa mabukhuwa akanalembamo nkhaniyi. Mwina bukhu la Mafumu linatsirizidwa kulembedwa zaka za 560 ndi 516 B.C.[8]

Mutu ndi Cholinga: Davide atamwalira (Mutu 1-2), mwana wake Solomoni anakhala mfumu. Mutu 1-11 akufotokoza za moyo ndi ufumu wa Solomo, kuphatikizapo kukwera kwa Israeli pa ulemererokufalikira kwa ufumu. Wa mapfuko, komanso kumangidwa kwa Kachisi ndi nyumba ya mfumu ku Yerusalemu. Koma zaka zomalizira za Solomoni anachoka mu dzanja la Mulungu chifukwa cha kulowelera ndi kupembeza mafano kwake, ndi kuleka kupembeza Mulungu mu Kachisi.

Chifukwa mfumuyi inali ndi malingaliro ogawanika, izi zinapangisanso ufumu wake kugawanika, kwa zaka 100 zotsatira bukhu la 1 Mafumu likulondola mbiri ya mafgulu awiri a mafumu ndi mapfuko awiri wa anthu osakhulupilira omwe amakhalu mu chikhalidwe chosiyana ndi cha Mulungu.[9]

Mfumu yotsatira inali Rehoboamu yemwe analandidwa dziko la kumpoto lomwe linali ndi mapfuko khumi ndipo limatchedwa isreali. Komanso dziko la kummwera lomwe linali ndi mapfuko awiri Benjamini ndi Yuda, lomwe limatchulidwa dziko la Yuda. Mu machaputala otsirizira a 1 Mafumu, nkhani yaikulu ndi ya zoipa zomwe mfumu Ahabu anachita ndi mneneri Eliya yemwe anadzudzula kuchimwa kwa Ahabu ndi kusamvera kwa Israeli.

Mutu weniweni ndi chofuna momwe kusamvera Mulungu kunatengera anthu mu kuwonongeka kwa ufumu. Chisamaliro ndi tsogolo la dzikoli chinagona pa kukhulupirika ndi kumvera Mulungu ndi mapangano omwe iye anapangana ndi Israeli. Bukhu la 1 Mafumu silinangolongosola za maina a mafumu kokha, komanso lakamba momwe mfumuyo kapena dziko lake linapambana kapena kulephera malingana ndi kukhulupilika kwake kwa Mulungu. Bukhu la Mafumu limafotokoza bwino za ***"momwe choonadi chimakwezera dziko, ndi momwe tchimo limaonongera ndikunyozetsa mtundu wa anthu"*** (Miyambo 14:34). Kusakhulupirika pa malonjezano a Mulungu, kumabweretsa kutha /kugonjetsedwa kwa ufumu ndi kugwidwa ukapolo.

Anthu: Solomo, Yeroboamu, Rehoboamu, Eliya, Elisa, Ahabu, Yezibeli

Khristu mu Nkhaniyi: Monga Davide, Solomo ndi mmodzi wa anthu omwe anasonyeza ukhristu mu chipangano chakale, kuonetsera Umesiya mtsogolo mwake, padziko lapansi. Solomo anachita izi, ndipo ulemelero wake, kulemekezedwa kwake ndi kutchuka kwake zonsezi zikunena za Khristu mu ulemelero wake pa dziko lapansi. Solomo akufaniziridwanso ndi Khristu kudzera mu nzeru zake zomwe anazichita.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Kuphatikizana kwa Maufumu: Zaka 40 mu Ulamuliro wa Solomo (1:1–11:43)**
   a. Kukwezeka kwa Solomo (1:1–2:46)

1:1-10	2:1-9	2:28-35
1:11-37	2:10-18	2:36-46
1:38-53	2:19-27	

   b. Nzeru za Solomo (3:1–4:34)

3:1-5	3:10-15	4:1-19
3:6-9	3:16-28	4:20-34

c. Solomo amanga Kachisi wa Yehova (5:1–8:66)

5:1-12	7:13-51	8:54-61
5:13-18	8:1-11	8:62-66
6:1-38	8:12-21	
7:1-12	8:22-53	

d. Kutchuka kwa Solomo (9:1–10:29)

9:1-9	10:1-13
9:10-28	10:14-29

e. Kuguga kwa Solomo ndi kugwa kwa ufumu wake (11:1-43)

11:1-13	11:14-40	11:41-43

2. Maufumu Agawikana: Zaka 80 Zoyambirira za Maufumu Awiri (12:1–22:53)

a. Chomwe chinayambitsa kugawikana kwa ufumu (12:1-24)

12:1-15	12:16-24

b. Yeroboamu akhala mfumu ya **Israeli** (12:25–14:20)

12:25-33	13:11-34
13:1-10	14:1-20

c. Yeroboamu mfumu ya **Yuda** (14:21-31)
d. Abiyamu mfumu ya **Yuda** (15:1-8)
e. Asa mfumu ya **Yuda** (15:9-24)
f. Nadabu mfumu ya **Israeli** (15:25-31)
g. Baasa mfumu ya **Israeli** (15:32–16:7)
h. Elahu mfumu ya **Israeli** (16:8-14)
i. Zimri mfumu ya **Israeli** (16:15-20)
j. Omori mfumu ya **Israeli** (16:21-28)
k. Ahabu mfumu ya **Israeli** (16:29–22:40)

16:29-34	19:1-8	21:11-29
17:1-16	19:9-21	22:1-12
17:17-24	20:1-12	22:13-28
18:1-19	20:13-25	22:29-40
18:20-35	20:26-43	
18:36-46	21:1-10	

l. Yehosafat mfumu ya Israeli **Yudah** (22:41-50)
m. Ahaziya mfumu ya **Israel** (22:51-53)

2 Mafumu

(Kubalalika–Tchimo Lochita Mwadala Limabweretsa Chitsiriziro Chowawa)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Pozindikira kuti bukhu la 1 ndi 2 Mafumu linali limodzi pachiyabi, ndipo kumapeto kwake linagawidwa, mlembi wa bukhuli angathe kukhala yemwe analemba bukhu la 1 Mafumu.

Zaka: 550 B.C. (werengani 1 Mafumu)

Mutu ndi Cholinga: Bukhu la 2 Mafumu likupitirira nkhani ya mneneri Eliya ndi woutsatira wake Elisa ndiponso likukamba a "nkhani ya Maufumu awiri" ndipo imapereka mbiri ya ufumu wa kumpoto wa Israeli ndi ufumu wa kuwera wa Yuda paka kufikira nthawi yowe aufuuwa anagonjetsedwa ndi kutengedwa ukapolo Israeli anagongetsedwa ndi Asuri mchaka ha 722 B.C. ndipo Yuda anagonjetsedwa ndi Baibulo mchaka ha 586 B.C. Koma kwa maufumu onse awiriwa, aneneri anali kuchenjeza anthuwo kuti ngati satembenukira kwa Mulungu, adzalangidwa komanso ufumu wawo sudzapitilira.

Bukhu la 2 Mafumu limati limatiphunzitsa kuti tchimo lochita mwadala limabweretsa chitsiriziro chowawa. Mu Bukhu la 1 ndi 2 Samueli pfuko (dziko) linabadwa ndipo mu 1 ndi 2 maufumu anagawikanandipo mu 2 Mafumu unawaikana ndi kubalalika. Aneneri atakhala zaka zochuruka kuwadandaulira anthu za kuti abwerere kwa Mulungu; iwowo sanamvere, choncho Mulungu anawalanga anthuwo monga momwe analonjezera. Popeza mabukhu onse awiriwa pachiyambi linali limodzi (1 ndi 2 Mafumu), onsewa analembedwa ndi cholinga chimodzi. Akutiphunzitsa za momwe kusakhulupilika kumabweretsa mkwiyo wa Mulungu mpaka kufika muyeso wogonjetsedwa ndi kulandidwa ufumu. Maufumu awiri onsewa anagwa chifukwa ha kulephera kwa amfumu kuti alamulire mwachilungamo.

Anthu: Eliya, Elisa, Yosiya, Naaan, Hezekiya

Khristu mu Bukhu la 2 Mafumu: Eliya mu bukhuli anali chithunzi cha mneneri wa Khristu, Yohane Mbatizi (Mateyu 11:14; 17:10-12; Luka 1:17). Elisa mu bukhuli, akutikumbutsa ife za Yesu Khristu ndipo Irving Jesen amalongosola motere:

> Eliya amadziwidwa ndi zochita zake, pomwe Elisa amadziwidwa chifukwa cha zozizwa zomwe anachita, zambiri mwa izo, zosowa za anthu. Utumiki wa Eliya ukutsindika za Chilamulo cha Mulungu, chiweruzo ndi madongosolo ena. Pomwe Eliya amangoonjezerapo izi pochita ntchito za chisomo cha Mulungu, chikondi ndi kupilira. Eliya anali ngati Yohane Mbatizi, wobvumbitsa mauthenga a kulapa machimo. Elisa anatsatira izi monga Khristu anatsatira Yohane. Kugwira ntchito ya chifundo kuchita zozizwa komanso kuonerera ndi kuchitira umboni kuti aneneri anali ochokera kwa Mulungu.[10]

Ryrie amalongosola 1 ndi 2 Mafumu motere:[11]

1 & 2 Mafumu	
1 Mafumu	**2 Mafumu**
Akuyamba ndi mfumu Davide	Akutha ndi mfumu yak u Baibulo
Akuyamba ndi ulemelero wa Solomoni	Akuthera ndi manyazi a Yehoakimu
Akuyamba ndi madalitso a kumvera	Akutsirizira ndi mateberero a kusamera
Akuyamba ndi kumanga Kachisi wa Mulungu	Akutseka ndi nkhani ya kuwotchedwa kwa Kachisi
Akuwunikira zotsatira zakuchita chisawawa	Akulongosola za zotsatira zakuchita chisawawa
Akuwonetsa momwe mafumu analephelera ku ulamuliro wa Mulungu	Akulongosola za zotsatira za kulepheraku
Akulongosola za mneneri Eliya	Akulongosola za mneneri Elisa
Akutsindika za kukhala wopilira ndi wofatsamwa Mulungu	Akutsindika za chilango cha Mulungu kwa ochimwa

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Kugawikana kwa Ufumu (1:1–17:41)**
   a. Ahaziya mfumu ya **Israel** (1:1-18)
   b. Yehoramu mfumu ya **Israel** (2:1–8:15)
      1) Chimasuliro cha Eliya (2:1-14)
      2) Kuyamba kwa utumiki wa Elisa (2:15-25)
      3) Yehoramu alimbana ndi a Moabu (3:1-27)
      4) Utumiki wa Eliya (4:1–8:15)

4:1-7	5:15-27	7:3-14
4:8-17	6:1-7	7:15-20
4:18-37	6:8-23	8:1-6
4:38-44	6:24-33	8:7-15
5:1-14	7:1-2	

   c. Yoram mfumu ya **Yuda** (8:16-24)
   d. Ahaziah mfumu ya **Yuda** (8:25-29)
   e. Yehu mfumu ya **Israel** (9:1–10:36)

9:1-13	9:33-37	10:34-36
9:14-26	10:1-17	
9:27-32	10:18-33	

   f. Athaliah mfumukazi ya **Yuda** (11:1-16)
   g. Yehowasi mfumu ya **Yuda** (11:17–12:21)

11:17-20	12:4-18
11:21–12:3	12:19-21

   h. Yehoahazi mfumu ya **Israel** (13:1-9)
   i. Yoasi (Joash) in **Israel** mfumu ya **Israel** (13:10-25)
   j. Amaziya mfumu ya **Yuda** (14:1-22)
   k. Yeroboamu II mfumu ya **Israel** (14:23-29)
   l. Azariya /Uzziya (Uzziah) mfumu ya **Yuda** (15:1-7)
   m. Zekariya mfumu ya **Israel** (15:8-12)
   n. Shallumu mfumu ya **Israel** (15:13-15)
   o. Menahemu mfumu ya **Israel** (15:16-22)
   p. Pekahiya mfumu ya **Israel** (15:23-26)
   q. Pekah mfumu ya **Israel** (15:27-31)
   r. Yotamu mfumu ya **Yuda** (15:32-38)
   s. Ahazi mfumu ya **Yuda** (16:1-20)

t. Hosea mfumu ya **Israel** (17:1-41)
   1) Kwa Israel (17:1-6)
   2) Tchimo la Israel (17:7-23)
   3) Israel amwazikana (17:24-41)

2. Ufumu wotsala wa Yuda (18:1–25:30)

a. Ufumu wa Hezekiya (18:1–20:21)

18:1-6	19:1-7	19:20-37
18:7-12	19:8-13	20:1-11
18:13-37	19:14-19	20:12-21

b. Ufumu wa Manasseh (21:1-18)
c. Ufumu wa Amon (21:19-26)
d. Ufumu wa Josiah (22:1–23:30)
e. Ufumu wa Jehoahaz (23:31-33)
f. Ufumu wa Jehoiakim (23:34–24:7)
g. The Reign of Ufumu wa Yehoiakin (24:8-16)
h. Ufumu wa Zedekiya (24:17–25:21)
   1) Baibulo Agalukiridwa / kuwonongedwa kwa Kachisi (24:17–25:10)
   2) Kutumizidwa kwachitatu kuchoka ku Baibulo (25:11-21)
i. Ulamuliro wa Gedaliah, wolamulira wopusa (25:22-26)
j. Kumasulidwa kwa Yehoiakin ku Baibulo (25:27-30)

1 Mbiri

(Kukonzekera za Kachisi)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Bukhu la Mbiri (1 ndi 2 Mbiri) poyamba linali bukhu limodzi. Bukhuli silikudziwika mlembi wake weniweni koma Ayuda amakhulupilira kuti Ezara ndiye mlembi wa bukhuli. Kukhazikika kwa kalembedwe ka bukhu limeneri, zikuonetsa kuti ngakhale kuti anthu ambiri anakhudzidwa potolera zoyenera kulembedwa m'bukhuli, m'lembi mmodzi ndi yemwe anamaliza kukonza bukhu lonse. Anthu ambiri akukhulupilira kuti, bukhuli linalembedwa ndi Samueli (1 Mbiri 29:29) Yesaya, (2 Mbiri 32:32), ndi ena ambiri (2 Mbiri 9:29; 12:15; 20:34; 33:19); koma makamaka pa zolembedwa za bukhu la Mafumu a aYuda ndi Aisrayeli (2 Mbiri 16:11; 25:26). Zolemebedwa za bukhuli zikuonetsa kuti analemba mwa unsembe chifukwa cha malingaliro a za mkachisi, unsembe, mbumba ya Davide komanso ufumu wa kumwera wa Yuda. Pali chikhulupiliro choti Ezara ndiye anatolera zonse za m'bukhuli, makamaka chifukwa pali nkhani zofanana pakati pa mabukhu a Ezara ndi Mbiri. Monga chitsanzo: nkhani yakumangidwa ndi kuperekedwa kwa Kachisi.

Ngakhale 1 ndi 2 Mbiri likulongosola za nthawi yofanana ya mbiri ya Ayuda; zolinga za mabukhuwa ndi zosiyana. Ngakhale zolembedwa zikuoneka zofananirapo, koma zikusonyeza kuti sakubwereza zolembazo ayi koma kuti akusonyeza mwa uzimu nthano ya pfuko la Israyeli. Mabukhu a Mafumu amapereka chiunikiro cha munthu, pomwe mabukhu a Mbiri amalongosola za chiunikiro cha Mulungu.

Mwachidule, mabukhuwa akungopereka kauniuni wambiri kuyambira pa Adamu mpaka nthawi yomwe pfukoli linatengedwa ukapolo ku Baibulo. Komanso mpaka pomwe Cyrus anagamula kuti anthuwa atulutsidwe ku ukapolo, ndikubwerera kwawo.[12]

M'mene anatanthauzira mawu a pa mpukutu, otanthauzirawa, anagawa bukhu la mbiri pawiri; 1 ndi 2 Mbiri, ndipo panthawiyi, bukhuli limatchedwa kuti bukhu la zinthu zomwe zinadumphidwa kapena kuiwalidwa' apa amatanthauza nkhani zomwe sizinalembedwe mu bukhu la Samueli ndi Mafumu. Dzina loti 'Mbiri', likuchokera ku mutu womwe Jerome anapereka mu Baibulo lomwe anatanthauzira mu chiLatini (A.D. 385-405). Jerome, potchula kuti Mbiri, ankatanthauza "mbiri ya nkhani zonse zokhuza chiyero."[13]

Zaka: 450–425 B.C.

Mutu ndi Cholinga: 1 Mbiri akulongosola mbiri ya kuchokera kwa Adamu, mpaka imfa ya mfumu Sauli. Ndipo mabukhu ena otsatirawo, akulongosola za ufumu wa Davide. Mabukhu a mbiri akuonetsa ngati akungobwereza zomwe zalembedwa mu mabukhu a Mafumu ndi Samueli. Koma ayi; bukhuli linangolembedwa ndi cholinga chofuna kukumbutsa anthu omwe anabwerera kwawo, kuchokera ku ukapolo wa ku Babulo, kuti iwowa anali mtundu wosankhika, mbumba ya Davide, anthu osankhidwa a Mulungu. Mbiri zones za mibadwo, zimaloza pa pangano la Davide, lomwe linalonjezedwa pa Abrahamu, kuti adzakhala kholo la pfuko, lomwe lidzadalitse maiko. Apa, mutu weniweni ndiwoti; "Mulungu ndi woona ndipo sazengereza ndi mapangano ake."

Mabukhu a Mbiri akutsindika za nthito ya chilamulo, unsembe ndi Kachisi ngakhale Kachisi wa Mulungu yemwe Solomo adamumanga anawerengedwanso monga mizu yolumikizidwa ndi nkhani za pachiyambi. Bukhuli likuphunzitsa kuti kale linali loyembekezera (la pathupi), kudikira kuti libereke za tsogolo. Chisawawa,

kupembeza mafano, kukwatira achikunja, komanso kusowa kwa umodzi, zinali zina mwa zifukwa zomwe ufumu wawo unasokonezeka. Ndi chinthu chosangalatsa kuti, atangochoka mu ukapolowo, Israeli sanapembezenso milungu ina ya chilendo, koma Yehova yekha.[14]

Anthu: Monga zakambidwa, ndi bukhu la Davide, ngakhale muli anthu ena monga mu bukhu la 1 Samueli monga Natani, Bathsheba ndi Uriah.

Khristu mu Bukhu la 1 Mbiri: Mu 1 ndi 2 Samueli pa nkhani ya David, ikuimilira Khristu.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **M'badwo Kuchoka kwa Adamu Kufika kwa Davide (1:1–9:44)**
   a. Adamu mpaka Abrahamu (1:1-27)
   b. Abrahamu mpaka Yakobo (1:28-54)
   c. Yakobo mpaka David (2:1-55)
   d. Davide paka Kugwidwa Ukapolo kwa Dziko (3:1-24)
   e. Mbadwo wa Mafuko Khumi ndi Awiri (4:1–8:40)

4:1-23	7:1-5	7:20-29
4:24-43	7:6-12	7:30-40
5:1-26	7:13	8:1-32
6:1-81	7:14-19	8:33-40

   f. Anthu okhala ku Yerusalemu (9:1-34)
   g. Banja la Sauli (9:35-44)

2. **Kukwera ndi Kudzodza kwa Davide (10:1–12:40)**
   a. Imfa ya Sauli (10:1-14)
   b. Kukwezedwa kwa Davide (11:1-3)
   c. Kulandidwa kwa Yerusalemu (11:4-9)
   d. Ziphona za Davide (11:10–12:40)

3. **Ufumu wa Davide (13:1–29:21)**
   a. Davide ndi Likasa la Yehova (13:1–17:27)
      1) Davide abweretsa Likasa ku Sidoni: Imfa ya Uzza (13:1-14)
      2) Kuitchuka kwa David ndi kugonjetsa kwake Afilisti (14:1-17)
      3) Davide abweretsa Likasa la Yehova ku Yerusalemu (15:1-29)
      4) Chikondwerero cha Davide ndi adongosolo a Likasa la Yehova (16:1-43)
      5) Davide afunisitsa kumanga Kachisi wa Yehova: Mapangano a Davide (17:1-27)
   b. Nkhondo za Davide (18:1–20:8)

18:1-17	19:10-19
19:1-9	20:1-8

   c. Davide achita kalembera, momuchimwira Yehova (21:1-30)
   d. Daide akonekera oanga Kachisi (22:1-23:1)
   e. Dongosolo la Davide pa Alevi (23:2–26:32)
      1) Chiwerengero ndi ntchito ya Alevi (23:2-32)
      2) Alevi agawidwa magulu 24 (24:1-31)
      3) Oyimbira (25:1-31)
      4) Alonda (26:1-19)
      5) Asungi chuma (26:20-28)
      6) Oweruza milandu mu khoti (26:29-32)
   f. Antchito a boma a Davide (27:1-34)
   g. Malangizo otsiriza a Davide pa anthu ake ndi pa Solomo (28:1-21)
   h. Davide apembeza Mulungu, nathiranso nsembe yopsereza (29:1-21)

4. **Imfa ya Davide, Solomo Alongedwa Ufumu (29:22-30)**

2 Mbiri

(Kuwonongedwa kwa Kachisi)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Monga tafotokoza kale; 1 Mbiri ndi 2 Mbiri anali bukhu limodzi; chonho monga tanena ku 1 Mbiri; mlembi weniweni sakudziwika koma aYuda amati ndi Ezara komabe kauniuni amafukula kuti mwina bukhuli linalembedwa ndi munthu mmodzi (wodziwa za mbiri). Pali mfundo zokwanira zotsimikizira kuti

mwina Ezara analembadi bukhuli chifukwa cha nkhani monga za Alevi ndi za Kachisi. Komabe ngakhale mlembi weniweni sakudziwika, koma wolembayo analongosola nkhani zopezeka mu:

1. Nkhani zopezeka mu bukhu la mafumu a Israeli ndi Ayudai (27:7; 35:27; 36:8)
2. Bukhu la Mafumu la Mafumu a Yuda ndi Israeli (16:11; 25:26; 28:26; 32:32)
3. Bukhu la Mafumu la a Israyeli (20:34; 33:18)
4. Nkhani za mbukhu la Mafumu (24:27)
5. Bukhu la Natani, uneneri wa Ariya, masomphenya a Iddo (9:29)
6. Mbiri ya Shemaiya (12:15)
7. Nkhani za Iddo (13:22)
8. Zolembedwa ndi mneneri Yesaya (26:22)
9. Zoyankhulidwa ndi Hozayi (33:19)
10. Maliro, madandaulo (35:25)
11. Zolembedwa ndi Davide ndi mwana wake Solomo (35:4)

Zaka: 450–425 B.C.

Mutu ndi Zolinga: Ngakhale nkhani za 1 ndi 2 Mbiri ndi za mu bukhu la Samueli, zikumasiyana mu zina; bukhu la 2 Mbiri akupitilizabe kufotokoza mbiri ya Davide monganso ku 1 ndi 2 Mafumu; Ndikofunikira kuti tidziwe kuti 1 Mbiri sanalongosole nkhani za ufulu wa kumpoto chifukwa anthu omwe anatsatira Davide anali osakhulupilira Mulungu ndipo 2 Mbiri ikulongosola bwino mafumu onse omwe analowa atafa Davide, onse osakhulupilira ndi okhulupilira Mulungu omwe. Chaputala 1 esi ya 9 chikulongosola a kumanga kacchisi mu nthawi ya Solomo pomwe pa 10:36; akuunikira ufumu wa kumwera mpaka pamapeto pake pamene yerusaleu anawonongedwa ndipo anthu onse anatengedwa ukapolo ku babulondipo bukhuli likupitilira kukamba za mafumu monga Asa, Yehosafati, Yowasi, Hezariya ndi Yosiya.

Omwe anabweretsa chitsitsimutso komanso kuti ana a pfukoli abwererenso kwawo kuchokera ku ukapolo; Bukhu la Mbiri silikulemba nkhani zonse mofanana ndi 1 ndi 2 Mafumu, koma zikumasiyana chilingaliro ndi chilongosolo ndi cholinga chotsindika pa zinthu zina. Mu 1 Mbiri, mutu wa nkhani ndi Davide, pomwe ku 2 Mbiri mutu wankhani ndi nyumba ya Davide. Mu bukhu la Mafumu, Mbiri ya mafuku yalembedwa kudzera pa mipando ya chifumu, pamene bukhu la mbiri lalembedwa kudzera ku guwa (Kachisi wa yehova). Mu bukhu la Mafumu, nyumba yachifumu ndilo mutu weniweni, pomwe ku bukhu la Mbiri, Kachisi wa yehova ndiye mutu wake weniweni. Mu bukhu lamafumu, akuwunikira pa mbiri ya ndale ya dziko pomwe mu bukhu la Mbiri akulongosola mbiri ya uzimu pa dziko la Israyeli.

Bukhu la mbiri ndilongolemba nthano. Izi ndi nkhani zomwe Mulungu akukumbutsa anthu pa kakhalidwe la uzimu mu ufumu wa Davide. Pa chifukwa cha ichi; akuunikira kwambiri pa ufumu wakumpoto wa Yuda, ndi ufumu wakumwera komwe kuli mafumu achitsitsimutso ndi oopa Mulungu mu mbadwo wa Davide, ndiponso akulongosola chifukwa chomwe ufumu wa kumpoto, womwe mafumu ake sanali owopa Mulungu, unakanthidwa ndi Mulungu.

Anthu: Yosiya, Rehoboamu, Solomo

Khristu mu Bukhuli la 2 Mbiri: Mpando wachifumu wa Davide unawonongeka, koma mbumba ya Davide idapitilira kukhalako. Anthu akupha, ozumzawo, achinyengo, nkhondo, ndi kugwidwa ukapolo; zonsezi zinaopseza ndi kusokoneza mbadwo wa mesiya, komabe unakhalapobe kuchokera pa Adamu mpakana Zerubabelo. Kukhwimitsa za Khristu kukuoneka mu mbiri ya mbadwo wake pa Mateyu 1 ndi pa Luka 3.[15]

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Ulamuliro wa Solomo (1:1–9:31)**
   a. Solomo adzodzedwa ufumu (1:1-17)

1:1-13	1:14-17	

   b. Kachisi wa Solomo (2:1–7:22)

2:1-10	5:1-10	7:4-7
2:11-18	5:11-14	7:8-10
3:1-2	6:1-11	7:11-22
3:3-17	6:12-42	
4:1-22	7:1-3	

   c. Kuchuka kwa Solomo (8:1–9:28)

8:1-18	9:1-12	9:13-28

   d. Imfa ya Solomo (9:29-31)

2. **Mfumu ya Yuda (10:1–36:21)**
   a. Rehoboamu (10:1–12:16)
      10:1-19 | 11:14-17 | 12:1-8
      11:1-13 | 11:18-23 | 12:9-16
   b. Abiya (13:1-22)
      13:1-3 | 13:4-19 | 13:20-22
   c. Asa (14:1–16:14)
      14:1-15 | 15:8-19 | 16:7-14
      15:1-7 | 16:1-6
   d. Yehosofati (17:1–20:37)
      17:1-2 | 18:28-34 | 20:14-19
      17:3-19 | 19:1-4 | 20:20-25
      18:1-7 | 19:5-11 | 20:26-34
      18:8-11 | 20:1-4 | 20:35-37
      18:12-27 | 20:5-13
   e. Yehoramu (21:1-20)
   f. Ahaziya (22:1–23:15)
      22:1-4 | 22:8-12 | 23:12-15
      22:5-7 | 23:1-11
   g. Yowasi (23:16–24:27)
      23:16-21 | 24:3-7 | 24:20-22
      24:1-2 | 24:8-19 | 24:23-27
   h. Amaziya (25:1-28)
      25:1-13 | 25:14-16 | 25:17-28
   i. Uzziya (26:1-23)
      26:1-5 | 26:6-15 | 26:16-23
   j. Yotamu (27:1-9)
   k. Ahaz (28:1-27)
      28:1-4 | 28:5-15 | 28:16-27
   l. Hezekiya (29:1–32:33)
      29:1-4 | 30:13-27 | 32:9-19
      29:5-19 | 31:1-2 | 32:20-33
      29:20-36 | 31:3-21
      30:1-12 | 32:1-8
   m. Manasse (33:1-20)
      33:1-9 | 33:10-20
   n. Amoni (33:21-25)
   o. Yowasi (34:1–35:27)
      34:1-7 | 34:22-30 | 35:20-27
      34:8-13 | 34:31-33
      34:14-21 | 35:1-19
   p. Yowahazi (36:1-4)
   q. Yehoiakimu (36:5-8)
   r. Yehoiachini (36:9-10)
   s. Zedekiyah (36:11-21)

3. **Chigamulo cha Koresi (36:22-23)**

Ezara

(Kumangidwanso kwa Kachisi ndi Kubwezeretsedwa kwa Anthu)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Ngakhale bukhu la Ezara silinalongosole bwino za mlembi wake, chikhalidwe cha chiYuda chimati Ezara ndiye mlembi wa bukhuli. Ezara analemba pogwiritsa ntchito mabukhu osiyanasiyana (4:16), mbiri za mibadwo (2:1-70), ndi nkhani zina za anthu (7:27–9:15).

Zoona ndi zakuti Ezara ndiye munthu yemwe anagwira ntchito yaikuru pakulemba bukhuli. Ezara anatengapo gawo lalikulu polemba bukhuli (1:10). Komanso mu 8:10 ya bukhu la Nehemiya.

Chiphunzitso chikunena kuti Ezara anali woyambitsa wa Sunagoge yaikuru (msonkhano waukulu) momwe munasonkhanidwa mabukhu a Chipangano Chakale. Mbiri ina, imamena kuti Ezara anatolera mabukhu onse a mubaibulo ndipo ndi iye yemwe anayambitsa kupembeza mu sunagoge.[16]

Mu nkhani ya Baibulo ya chi Levi; Ezara ndi Nehemiya linali bukhu limodzi. “Bukhu la Ezara.” Mabaibulo akale achihebri, anasanja mabukhuwa mosiyanitsa Ezara ndi Nehemiya mu chinenero cha chingerezi. Pomaliza, Josephus (wolemba mbiri wa chiyuda), ndi Jerome (mlembi wachiLatini), anawatenga mabukhuwa ngati bukhu limodzi.

Zaka: 457–444 B.C.

Mutu ndi Cholinga: Malinga ndi mbiri, Ezara anapitilira kumasulira kuchokera pomwe 2 Mbiri anathera ndipo anaunikira mbiri ya kubwerera kwa aYuda kuchokera kuukapolo ku Babulo, ndikumanganso Kachisi.Malinga ndi maunikidwe a uzimu ndi chiphunzitso, Ezara anaonetsera momwe Mulungu amakwaniritsira malonjezano ake pa anthu ake, ku dziko lamalonjezano patatha zaka 40 za muukapolo, komanso mwa maulosi a aneneri. Monga mu mbiri, Ezara wansembeyo, amasonyeza kufunika kwa Kachisi ndi mapembezedwe a anthu mukachisi, miyoyo yawo mu pfuko lawo monga ana a Mulungu. Anthuwa anamanga Kachisi mwa chimwemwe ndi mokondwera koma anachedwetsedwa kwa zaka 18 ndi adani awo ochokera ku mpoto. Potsiriza chigamulo cha Dariyo, chinawaloleza kuti amalizitse kumanga kachisisiyo (Ezara 1–6). Ezara 7–10 amatiuza za kubwerera kwa wansembe Ezara yemwe ankaphnzitsa anthu, za chilamulo ndi pfuko lokonzedwanso mu moyo wauzimu.

Mutu wa bukhuli ungathe kukhala wa uzimu, wakuthupi, komanso wa chisamaliro cha anthu obwerera kuchokera kuukapolo mu ulamuliro wa Zerubabelo ndi Ezara.

Anthu: Koresi (mfumu ya a Perezi yemwe analoleza kuti abwerere kuchokera ku ukapolo), Ezara (wansembe ndi mlembi), Jeshua (wansembe wamkulu), Zerubabelo

Khristu mu Bukhuli la Ezara: Posunga pangano la Davide ndi malonjezano a Mulungu monga mbuba ya tiri amoyo chifukwa cha Mesiya, Mwana wa Davide; ndipo Ezara ndi Nehemiya akutionetsa m’mene Mulungu anapitilira kusunga malonjezano ake pakubweretsa anthu ku dziko lawo la malonjezano.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Kubwezeretsedwanso: Abwerera Koyamba (Kwawo) Pansi pa Ulamuliro wa Zerubabelo (1:1–6:22)**
   a. Chigamulo cha Koresi (1:1-11)
      1:1-4 1:5-11
   b. Kalembera wa anthu (2:1-70)
      2:1-35 2:40-60
      2:36-39 2:61-70
   c. Ayamba Kumanga Kachisi (3:1-13)
      3:1-7 3:8-13
   d. Chisutso (4:1-24)
      4:1-7 4:8-16 4:17-24
   e. Mamangidwe achitikanso (5:1–6:12)
      5:1-5 5:6-17 6:1-12
   f. Atsiriza kumanga Kachisi (6:13-22)
      6:13-18 6:19-22

2. **Kukonzedwanso kwa Anthu; Abwereranso Motsogozedwa ndi Ezara (7:1–10:44)**
   a. Abwerera ku Yerusalemu (7:1–8:36)
      7:1-10 8:1-14 8:33-36
      7:11-26 8:15-20
      7:27-28 8:21-32
   b. Chitsitsimutso ku Yerusalemu (9:1–10:44)
      9:1-4 10:1-17
      9:5-15 10:18-44

Nehemiya
(Kumangidwanso kwa Linga)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Ngakhale anthu ena amakhulupilira kuti bukhuli analemba ndi Nehemiya, chifukwa cha mau a pa 1;1; ***“mawu a Nehemiya mwana wa Hikaliya”*,** koma ena amakhulupilira kuti bukhuli linalembedwa ndi Ezara yemwe anagwiritsa ntchito mawu ochokera kwa Nehemiya. Komanso gulu linanso la anthu likukhulupilira kuti bukhuli linalembedwa ndi Nehemiya chifukwa nkhani zambiri zolembedwa mubukhuli zikulongosola za anthu omwe anakumana ndi Nehemiya pamoyo amene akukhudzana ndi kubwerera ku Yerusalemu (1:1–7:73; 12:31–13:31).[17]

Ngakhale likuoneka kuti bukhu la Nehemiya ndi Ezara linali limozdi pachiyambi; gawo lotsiriza la bukhuli linatchulidwa dzina loti Nehemiya yemwe anali wothandizana ndi Ezara komanso woperekera chikho kwa Koresi mfumu ya aPerezi. Dzina loti Nehemiya litanthauza kuti Yehova atonthoza ndi kulimbikitsa.

Zaka: Nkhani zambiri za mu bukhuli zikusonyezazanso nkhani za mu Ezara ndi Nehemiya, kusonyeza kuti linalembedwa mu zaka za **445 B.C. - 425 B.C.**

Mutu ndi Cholinga: Bukhuli likupitilira kunena za mbiri ya aYuda mu nthawi yomwe anabwera kuchokera ku ukapolo Nehemiya anasiya ntchito yoperekera chikho kwa Aritasasta, mfumu ya a Perezi ndikukhala mdindo wolamulira Yerusalemu, ndipo pa ulamuliro wake iye anatsogolera anthu kukmanganso linga la mzindawo. Nthawi ya Ezara ndi Nehemiya inali yofanana (Nehemiya 8:2, 9) ndipo onse anali atumiki a Mulungu omwe anamutumikira YAHWEH mu nthchito zosiyanasiyana, pomwe Ezara anali wansembe ndi wokangalika kutumikira za uzimu, Nehemiya anali munthu wandale yemwe anatsogolera ngati mdindo pa ntchito yakumanganso linga la ku Yerusalemu. Bukhu la Nehemiya linbalembedwa pofuna kutionetsera za mkono wa Mulungu, kudzera mu kubwereranso kwawo kwa pfukoli kuchokera kuukapolo. Pa ulamuliro wa Nehemiya, pa masiku 52, anakwanitsa kuchita zinthu zomwe zinalephereka kuchitidwa kwa zaka 94, kuchokera pa kubwerera kwawo koyamba pansi pa Zerubabelo. Kudzera mu kumvera ndi chikhulupiliro, anakwanitsa kupyola ndi kugonjetsa zitsutso ndi zipsinjo zones.[18]

Anthu: Nehemiya, Aritastata, Sanibalati, Ezara

Khristu mu Nkhaniyi: Nehemiya akutionetsa chifundo cha Khristu posiya mpando wake wachifumu, ndikudzagwira ntchito yakubwezeretsanso anthu muchimake. Chigamulo cha Aristata, chikusonyeza chiyaambi cha ulosi wa Daniel wamasabata 70 kuchokera pakubweranso kwa mesiya (Danieli 9:25-27).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Kumangidwanso kwa Khoma (1:1–7:73)**
   a. Kukonekera a kuanganso (1:1–2:20)

1:1-11	2:1-10	2:11-20

   b. Kuanganso (3:1–7:73)

3:1-32	5:1-13	6:15-18
4:1-8	5:14-19	7:1-65
4:9-23	6:1-14	7:66-73

2. **Kubweeretsedwanso kwa Anthu (8:1–13:31)**
   a. Kubwereedwa kwa Pangano (8:1–10:39)

8:1-8	8:13-18	10:1-27
8:9-12	9:1-38	10:28-39

   b. Anthu aera Pangano (11:1–13:31)

11:1-19	12:27-30	13:10-14
11:20-36	12:31-47	13:15-22
12:1-21	13:1-3	13:23-31
12:22-26	13:4-9	

Estere

(Chitetezo kwa Anthu a Mulungu)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Bukhu la Estere limalongosola bwino za yemwe analemba bukhuli. Izi zikutsimikizira kuti mlembiyu anali munthu wokhuzidwa mu nkhaniyi, komanso muyuda. Anthu ena amalongosola kuti Ezara kapena Nehemiya ndiwo analemba bukhuli.[19]

Bukhuli limatenga dzina lake kuchokera pa mwini nkhani yemwe dzina lake m'chihebri linali Hadassah (Myrtle) ndipo linasinthidwa kukhala Estere (chiyankhulo chachiperesi), ndipo Estere amatanthauza nyenyezi.

Zaka: Nkhani za pakati pa chaputala cha 6 ndi 7 cha esitere zinachitika mu nthawi yomwe pfukoli limachokera kuukapolo muulamuliro wa Zerubabelo, komanso muulamuliro wa Ezara. Bukhu la esitere linalembedwa mzaka za **470-465 B.C.** komanso pa ulamuliro wa Ahasiwero (10:2-3), ndi ulamuliro wa mwana wa Ahasiwelo, Aritastata (464-424 B.C.).

Mutu ndi Cholinga: Bukhuli limakamba za msungwana wina yemwe mfumu Ahaziwero ya peresi anamusankha kukhala mkazi wake. Pamene Hamani anakonza chiwembu chofuna kupha Ayuda, Mordekai

msuweni wa Estere anakakamiza Estere kuti apulumutse anthu a mtundu wake. Estere analimba mtima, nalankhula ndi mfumu za nkhaniyi, ndipo anthu anapulumuka. Ngakhale bukhu la Estere ndi bukhu limodzi lokhalo mu Baibulo limwe silatchule dzina loti Mulungu. Mutu ndi cholinga cha bukhuli unali wofuna kuonetsa chiombolo cha Mulungu pa anthu ake munthawi ya chipsinjo ndi mayesero.

Anthu: Estere, Hamani, Modekai, Hamani, Ahaziwero

Khristu mu Bukhu la Estere: Bukhuli likupereka chithunzi cha Khristu makamaka pamene iye akulolera kuphedwa kuti anthu ake apulumuke komanso Estere anakhala mkhalapakati wawo. Tikuonanso kuti Mulungu anapitilira kuteteza a Yuda, ndipo kudzera mu pfuko la aYudali, Mesiya anabwera.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Zoopsa kwa Ayuda (1:1–3:15)**
   a. Esitere asankhidwa kukhala mkazi wa Mfumu Vasiti (1:1–2:23)
      1:1-9 | 2:1-7 | 2:17-20
      1:10-22 | 2:8-16 | 2:21-23
   b. Haman achita chiwembu pa Ayuda (3:1-15)

2. **Ayuda Awomboledwa (4:1–10:3)**
   a. Ganizo la Esitere pa Ayuda (4:1–5:14)
      4:1-8 | 4:15-17 | 5:9-14
      4:9-14 | 5:1-8
   b. Hamani agonjetsedwa (6:1–7:10)
      6:1-9 | 7:1-6
      6:10-14 | 7:7-10
   c. Chigamulo cha mfumu Ahasiwero ndi Modekayi (8:1-17)
      8:1-8 | 8:9-17
   d. Adani a Ayuda agonjetsedwa (9:1-19)
      9:1-10 | 9:11-19
   e. Masiku a phwando la Purimu (9:20-32)
   f. Modekai alengezedwa ndi kukwezedwa dziko lonse (10:1-3)

Gawo 3
Mabukhu a Ndakatulo

Malonje: Mu kauniuni wa mabukhu oyambirira 17 (a chilamulo ndi mbiri) omwe tawalongosola kale, kuyambira Genesis mpaka Nehemiya takamba mbiri yonse ya muchipangano chakale. Mabukhu ena otsatira ndi a ndakatulo ndi ena a aulosi amene akulumikizana bwino ndi mabukhu onse 17 oyabirira aja. Mtsogolomu, tikhala tikukambirana za mabukhu asanu a ndakatulo omwe ndi awa–Yobu, Masalimo, Miyambo, Mlaliki ndi Nyimbo ya Solomo. Tisanayambe kuyang'ana mabukhu amenewa bwinobwino, tiyenera kuona za chikhalidwe cha mabukhu onse asanu amenewa. Ophunzira ayenera kumvetsa bwino kuti mau oti "ndakatulo" amakamba za kalembedwe kokha basi. Izi sizikutanthauza kuti izi ndizolembedwa monga mwa maganizo a anthu. Mabuku amenewa amaonetsa zenizeni zimene anthu akumana nazo m'moyo wawo.

Ubale/Kulumikizana: Mabukhu 17 aja ndi ambiri, koma awa 5 ndi a ndakatulo, ndipo akulongosola nkhani zomwe zinachitikira anthu ena. Mabukhu ambiri amakhuza nkhani za pfuko, koma mabukhu awa a ndakatulo akulongosola za makhalidwe ndi maonekedwe a anthu. Mabukhu a ndakatulowa akulimbana ndi mtima wa munthu pomwe mabukhu ambiri amalimbana ndi pfuko la chihebri.

Mabukhu a ndakatulowa si okhawo omwe akunena za ndakatulo mu chipangano chakale; mabukhu enanso a ulosi aatha kukhala ndakatulo chipangano chakale chinagawidwa magulu anayi:

1. Chilamulo–amakamba za moyo wathupi wa ana a Israyeli
2. Mbiri–amakamba a chitukuko cha dziko la Israeli ndi moyo wawo
3. Ndakatulo–amakamba za moyo wauzimu wa Israyeli
4. Mauloso–amakamba za moyo wa tsogolo wa Israyeli ndi kukwaniritsidwa kwa kubwera kwa Mesiya

Mabukhu Asanu a Ndakatulo:

1. Bukhu la Yobu–Madalitso Pambuyo pa Zipsinjo
2. Masalimo–Kuukweza Yehova Kudzera mu Pemphero
3. Miyambo–Nzeru
4. Mlaliki–Choonadi
5. Nyimbo ya Solomo–Chimwemwe Kudzera mu Umodzi

Nthawi ya Ndakatulo za a Hebri: Ngakhale ndakatulo za chihebri zinalembedwa mu mbiri ya chipangano chakale chonse, pali nyengo zitatu zodziwika bwino za mu nthawi ya ndakatulozi:

1. Nthawi ya Makolo/ Matate–Yobu (1750 B.C.)
2. Nthawi ya Davide–Masalimo (1050 B.C.)
3. Nthawi ya Solomo–(950 B.C.)
   a. Nyimbo za Solomo–chikondi cha mzibambo
   b. Miyambo–nzeru ya mkulu
   c. Mlaliki–chisoni cha nkhalamba (950 B.C.)[20]

Khristu mu Mabukhu a Ndakatulo: Monga takhala tikukamba mbuyomu, Khristu ndiye mtima weniweni wa Baibulo. Poyankha ophunzira aja pa njira yaku Emau; mmene iwo anakhumudwa ndi kuzunguzika pa kupachikidwa; imfa; ndi kuukanso m'manda; Yesu analonjeza bwinobwino nkhani yokhudza Iye mwini kudzera mu bukhu lopatulika (Luka 24:27). Ndipo pambuyo pake Iye anaonekera kwa akuphunzira khumi ndi mmodziwo nati: ***"Awa ndi mawuwo ndinalankhula nanu paja ndinakhala ndi inu, kuti ziyenera kukwaniritsidwa zones zomwe zinalembedwa za ine mu chilamulo cha Mose, ndi aneneri, ndi Masalimo"*** (Luka 24:44).

Polingalira izi, mungathe kuona kuti ndichinthu chabwino kuti powerenga bukhu lirilonse la ndakatulo, muzikhala ndi malingaliro a Khristu. Ndipo polingalira izi, Norman Geisler analemba kuti:

> Pamene maziko anayalidwa ndi Khristu pa Chilamulo, ndi kukonzekeranso kwa Khristu kumene kunaonetsedwa mu mu mabukhu a Mbiri, mabukhu a ndakatulo abvumbulutsa kufunikira kwa Khristu m'mitima mwa anthu. Mabukhu andakatulowa amalimbikitsa za moyo wokwaniritsidwa mwa Khristu mu njira yapadera-dera, molingana ndi chidziwitso cha munthu kapena ai.[21]

Yobu akutionetsera kufunika kokhala ngati nkhalapakati wa Khristu. Miyambo ikuonetsa kufunikira kwa nzeru mwa Khristu. Mlaliki akuonetsa kufunikira kwenikweni kokhutitsidwa ndi zinthu. Nyimbo ya Solomo ikutionetsera kufunika kokhala mu umodzi m'chikondi cha Khristu.

Ndakatulo za Chihebri

Maonekedwa a Ndakatulo za Chihebri: Bukhu la ndakatulo za chiYuda ndi zosiyaniranako ndi zina za Chingelezi zimene zimakhala ndi mizere ya nkhani zofananirako. Ndakatulo zachiYuda ziri ndi chikhalidwe chake chimene chimapangitsa anthu kuphunzira kanthu kena kake. Pali kufanana (kumene kumaonekera ndi mizere ina ya zolembedwazo) kumene kumaonetsa chikhalidwe chenicheni cha ndakatulo za Baibulo.

Mitundu itatu ya Ndakatulo za mu ChiHebri: Ndakatulo za nyimbo, zomwe zimalembedwa ngati nyimbo zoyimbidwa ndi mawu komanso zida monga kaligo. Izi zimatchedwa Masalimo: (1) Ndakatulo za chiphunzitso zomwe pogwirita ntchito mawu a choonadi (Masalimo); (2) zimaphunzitsa mfundo zenezeni za pamoyo wa munthu (Miyambo, Mlaliki); (3) Ndakatulo za msekeretso/zosangalatsa zomwe zimagwiritsidwa ntchito polumikizana ndi kupereka uthenga (Yobu ndi Nyimbo ya Solomo).

Mbali Ziwiri Zodziwika Bwino Mu Ndakatulo Za Chihebri: Zifanifani ndi Zining'a

Zifanifani

Ndakatulo zachiHebri zimabwereza ndi kusanjanso malingaliro. Zifanifani ndiwo mawu ofananitsa ndi mawu anzake. Pali itundu isanu ya kasanjidwe ka ndakatulozi.

A. Mawu Ofanana–Ganizo la mzere woyamba, likutsindikidwa pa ganizo lamzere wachiwiri (Masalimo 2:4; 3:1; 7:17).
B. Mawu a Mtsutso–Ganizo la mzere woyamba, likutsindikidwa motsutsana ndi la mzere wachiwiri (Masalimo 1:6; 34:10) ndipo mawu oterewa amadziwika ndi mawu oti, "koma, pomwe"
C. Mawu Ophatikizana–Mzere woyamba umalongosola mophatikizana ndi mzere wachiwiri (Masalimo 1:3; 95:3).
D. Mawu a pa Mpondachimera (otsimikiza) –Mzere wachiwiri ukubwereza motsindika moikiridwa m'mang'ombe ndi mzere womaliza (Masalimo 29:1).
E. Mawu a Chizindikiro–Mawu a nzere oyamba amanena chindunji cha nkhani, mzere wachiwiri umanena mokuluwika, mopereka chithunzithunzi (Masalimo 42:1; 23:1).

Zining'a

Zining'a ndi mawu omwe amanenedwa poimirira mawu ena. Ndakatulo za chiHebri zigwiritsanso ntchito zining'a poyankula zina ndi zina.

Mwachitsanzo ***"Woyenda mu choonadi cha Ambuye akunga mtengo wookedwa pa ntsinje"*** (Masalimo 1:2-3). Woyenda mu choonadi; si mtengo ayi koma akufanana ndi mtengo wookedwa m'bali mwa madzi (Masalimo 5:12; 17:8; 131:2). Mukhonza kupeza mau ngati, "monga" kapena "ngati" mu zolankhura zamtundu umenewu (Masalimo 5:12; 17:8; 131:2).

Mawu ena a chining'a amafananiza chinthu china ndi china pogwiritsa ntchito mau oti "ndi". Pa Masalimo 23:1 Davide akuti ***"Yehova ndiye mbusa wanga"*** apa sizisonyea kuti Davide anali chirombo cha miyendo inayi monga nkhosa; mbuzi kapena n'gombe ayi; koma ali ndi chitsimikizo kuti Yehova amasunga ndikusamalira moyo wake monga m'busa asamalira nkhosa (Masalimo 84:11; 91:4).

Palinso zining'a zina zonena moonjezera mawu pofuna kutsimikizira chinthu. Masalimo 6:6, Davide anati, ***"ndiyandamitsa kama wanga usiku wonse, mphasa yanga ndiyonyowa ndi misonzi yanga."*** Apa zikungosonyeza kuti Davide anali wodzazidwa ndi chisoni. Sizimatanthauza kuti Divide analira kwambiri mpaka misonzi yake inadzadza muchipinda chonse ndikuyandamitsa kama wake ayi (Masalimo 78:27; 107:26).

Nthawi zina mu mabukhuwa, funso limatha kuimirira yankho kapena kutambasula mawu, chitsanzo: ***"Afanana ndi Inu ndani?"*** (Masalimo 35:10). Cholinga cha Davide chinali chotsindika za ukulu wa Mulungu, osati amangoyembekezera yankho yankho loti "palibenso wina," ayi (Masalimo 56:8; 106:2).

Potsiriza, chitsanzo china ndi chogwiritsa ntchito chiwalo cha nyama, pofuna kutanthauza munthu. Izi zimachitika pofuna kulongosola bwino choonadi cha Mulungu (Masalimo 17:8). Davide akufunsa Mulungu ***"Ndifungatireni mu mthunzi wa mapiko Anu."*** Apa samatanthauza kuti Mulungu ndi mbalame ayi, koma amatanthauza kuti Mulungu amasungu munthu mu mpumulo wabwino, ndipo iye amapempha Mulungu kuti amuteteze monga momwe Mbalame imachitira kwa ana ake (Masalimo 91:4).

Yobu
(Madalitso Atatha Masautso)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Ngakhale dzina la bukhuli likuchokera pa dzina la mwini nkhaniyi, (Ezekieli 14:14, 20; Yakobo 5:11), mlembi weniweni wa bukhuli sakudziwika. Anthu ena amati Yobu, ena Elihu, ena Mose, Solomoni, ndi ena ambiri, ndiwo amene analemba bukhu la Yobu. Kuyambira mu nthawi ya Abrahamu, Isaki, Yakobo ndi Yosefe; bukhuli linatenga dzina lake kuchokera kwa mwininkhani wotchedwa Yobu, yemwe atatha kukumana ndi umphawi, mavuto a mbanja ndi zipsinjo za thanzi lake, anakhalao anawona ukulu wa Abuye.

Zaka: Ngakhale mlembi weniweni sakudziwikanso; nthawi yeniyeni yolembedwa bukhuli siyikudziwikanso koma nkhani ya Yobu inachitika mu zaka za 1445–1405 B.C mu nthawi yakuperekedwa kwa malamulo khumi kwa Mose. Ndipo tikuonanso kuti isanafike nthawi yolandira malamuloyi inali nthawi yomwe ansembe ankathira nsembe yopsereza ndipo tikuonanso kuti Yobu anathira nawo nsembe (Yobu 1:5) kuthirira mbumba yake choncho izi zikusonyeza kuti nkhani ya Yobu inachitika nthawi ya Abrahamu; malamulo asanaperekedwa kwa Mose.

Mutu ndi Cholinga cha Bukhu: Bukhuli likutionetsa Chiombolo cha Mulungu, ubwino ndi chilungamo chake komanso kupezeka kwake pamene anthu ali mu m'mavuto komanso ndikufulira kwa Iye. Bukhuli linalimbana ndi funso loti; chifukwa chiyani anthu okhulupilira Mulungu amavutikanso ngati Mulungu ali wachifundo ndi chikondi? Bukhuli limatiphunitsa za kupezeka kwa Mulungu pamene munthu wamuvomereza ndikumupempha. Anzake a Yobu atatu; anali ndi yankho limodzi lofanana koma lolakwika, iwo amati munthu umapeza mavuto chifukwa wachimwira Mulungu. Koma Elihu anati, mavuto amabwera pofuna kutsuka munthu. Choncho, cholinga cha Mulungu ndi choti amukhazikitse kupitilira kumukhulupilira ndi kudalira Mulungu nthawi zonse, pamavuto, kaya pamtendere. Archer analongosola a bukhu la Yobu:[22]

> Bukhu ili limatiphunzitsa poyankha funso loti; chifukwa chiyani okhulupilira amakumananso ndi mavuto? (1) Mulungu ndi wachikondi, chikondi chake choposera madalitso; (2) Mulungu angathe kuvomereza chipsinjo kubwera mwa munthu ndi cholinga chofuna kukulitsa chikhulupiliro cha munthuyo; (3) Maganizo a Mulungu ndi ozama koposa a munthu. Choncho iye amadziwa zoyenera kupanga, ndi nyengo yake, malinga ndi zifukwa zomwe iye mwini amadziwa. Izi zikutsutsana ndi maganizo a anzake a Yobu aja: Elihu, Bilidadi ndi Zopari.[23]

Cholinga china cha bukhuli chinali chofuna kutionetsa mkangano pakati pa Satana ndi Mulungu, ndipo Satana amagonja kumapeto kwa zonse, popeza Mulungu ndiye choonadi Aroma 8:28.

Anthu: Yobu, munthu woongika, wopanda tchimo, woopa ndi kukhulupilira Mulungu; anzake a Yobu–Elihu, Zoperi, Bilidadi, Elifazi, Satana

Khristu mu Nkhani ya Yobu: Mu bukhuli, Khristu akuonekera mu njira zingapo. Yobu akubvomereza Momboli (19:25-27) ndi Yobu akupempherera mkhalapakati (9:33; 33:23) iye akudziwa kuti akusowekera wina woti amulongosolere bwino za zinsinsi za Mulungu pa zipsinjo zake, ndipo yankho lake ndi Khristu yemwe amadziwa zovuta zathu, ndipo amagongetsa zones (Ahebri 2:14-18; 4:15; Aroma 8:32-34).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Chiyambi: Zipsinjo za Yobu (1:1–2:13)**
   a. Masautso ndi makhatidwe (1:1-5)
   b. Mavuto ndi kochokera kwake-Satana (1:6–2:10)
      1:6-12 1:13-22 2:1-10
   c. Anthu omutonthoza (2:11-13)

2. **Atsutsana ndi Zonena za Anzake Atatu Aja (3:1–31:40)**
   a. Mtsutso woyamba (3:1–14:22)
      1) Kulira kwa Yobu (3:1-26)
         3:1-19 3:20-26
      2) Yankho la Elifazi (4:1–5:27)
         4:1-11 5:1-7 5:17-27
         4:12-21 5:8-16
      3) Yobu ayankha Elifazi (6:1–7:21)
         6:1-7 6:24-30 7:11-21
         6:8-13 7:1-6
         6:14-23 7:7-10

4) Bilidadi ayankha (8:1-22)

8:1-7	8:8-10	8:11-22

5) Yobu atsutsana ndi Bilidadi (9:1–10:22)

9:1-12	9:25-35	10:8-17
9:13-24	10:1-7	10:18-22

6) Zapori ayankhulapo (11:1-20)

11:1-6	11:7-12	11:13-20

7) Yobu ayankha zapori (12:1–14:22)

12:1-6	13:13-19	14:13-17
12:7-12	13:20-28	14:18-22
12:13-25	14:1-6	
13:1-12	14:7-12	

b. Mtsutso wachiwiri (15:1–21:34)

1) Elifazi ayankha (15:1-35)

15:1-16	15:17-35

2) Yobu ayankha (16:1–17:16)

16:1-5	16:18-22	17:6-16
16:6-17	17:1-5	

3) Bilidadi ayankha (18:1-21)

18:1-4	18:5-21

4) Yobu ayankha (19:1-29)

19:1-6	19:7-22	19:23-29

5) Zapori ayankhulapo (20:1-29)

20:1-11	20:12-19	20:20-29

6) Yobu ayankha (21:1-34)

21:1-16	21:17-26	21:27-34

c. Mtsutso wachitatu (22:1–31:40)

1) Elifazi ayankha (22:1-30)

22:1-11	22:12-20	22:21-30

2) Yobu ayankha (23:1–24:25)

23:1-7	24:1-12	24:18-25
23:8-17	24:13-17	

3) Bilidadi ayankha (25:1-6)

4) Yobu ayankha (26:1–31:40)

26:1-4	29:1-20	31:9-12
26:5-14	29:21-25	31:13-15
27:1-6	30:1-8	31:16-23
27:7-12	30:9-15	31:24-28
27:13-23	30:16-23	31:29-37
28:1-11	30:24-31	31:38-40
28:12-22	31:1-4	
28:23-28	31:5-8	

3. Mawu a Elihu (32:1–37:24)

a. Mawu oyamba: Mulungu alangiza munthu kudzera mu zipsinjo (32:1–33:33)

32:1-10	33:1-7	33:19-22
32:11-14	33:8-12	33:23-28
32:15-22	33:13-18	33:29-33

b. mawu achiwiri: chilungamo cha Mulungu chawonekera (34:1-37)

34:1-9	34:16-20	34:31-37
34:10-15	34:21-30	

c. Mawu achitatu: kufunika kokhala olungama ndi oyera mtima (35:1-16)

35:1-8	35:9-16

d. Mawu achinayi: Ukulu wa Mulungu ndi kukanthidwa kwa Yobu potsutsa Mulungu (36:1–37:24)

36:1-16	36:24-33	37:14-20
36:17-23	37:1-13	37:21-24

4. Bvumbulutso la UMulungu-Mphepo (38:1–42:6)

a. Bvumbulutso Loyaba (38:1–40:5)

1) Mphamvu za Mulungu zikuonekera pa chilengedwe (38:1–39:30)

38:1-7	38:25-30	39:5-12
38:8-11	38:31-33	39:13-18
38:12-15	38:34-38	39:19-25
38:16-18	38:39-41	39:26-30
38:19-24	39:1-4	

2) Yobu azitsutsa navomereza machismo ake (40:1-5)

b. Bvumbulutso lachiwiri: mphamvu za Mulungu ndi kufooka kwa munthu; Yankho lozichepetsa la Yobu (40:6–42:6)

40:6-9	40:19-24	42:1-6
40:10-14	41:1-11	
40:15-18	41:12-34	

5. Ndemanga Yomaliza (42:7-17)

a. Yobu atsutsa mabwenzi abodzawo (42:7-9)

b. Zonse za Yobu zibwezeretsedwanso (42:10-17)

Masalimo

(Chiyamiko Kudzera mu Pemphero)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Bukhu la Masalimo ndi bukhu lalitali kuposa mabukhu onse, komanso lomwe limagwiritsidwa ntchito kwambiri chifukwa cha malembedwe ake. Chisoni chikusanduka chimwemwe, kuimba kukukhala pemphero ndi pembedzero. Ngakhale mwambiri sanalongosole mlembi wa bukhuli, koma zigawo za Masalimo zimatchula alembi motere:[24]

Alembi a Bukhuli		
Davide	78	Masalimo 1-41; 51-70; 86; 103; 108-110; 122; 124; 131; 133; 138-145
Asaph	12	Masalimo 50, 73-83
Korahite	12	Masalimo 42-49; 84-85; 87-88
Solomo	2	Masalimo 72, 127
Mose	1	Masalimo 90
Ethan	1	Masalimo 89
Anthu ena osadziwika maina	44	Masalimo 71; 91-102; 104-107; 111-121; 123; 125-126; 128-130; 132; 134-137; 146-150

Ku chiyankulo cha chiHebri bukhu la Masalimo limatchedwa “matamando,” “bukhu lamatamando.” Ndi Masalimo 145 okha omwe alembedwa mmonga “matammando,” matamando mkati mmwa nyimbo. Masalimo ndi nyimbo ndi ndakatulo zachihebri ndipo mawu oti Masalimo atanthauza kuimba ndi zida za zingwe.

Zaka: Pokamba za chaka chomwe Masalimo analembedwa, Gleason Archer anati:

> Mwa zonsezi, Salimo lakale kwambiri ndi Masalimo 90, lomwe linalembedwa ndi Mose mu 1405 B.C. Masalimo a Davide analembedwa zaka za 1020–975 B.C., a Asath, mchaka cha 950 B.C. Kora ndi ana ake, zaka zake sizikudziwika bwino. Masalimo opanda dzina la mlemmbi, mwina analembedwa ndi Davide, monga awa 2, ndi 33, ndi enanso ataturuka ku ukapolo 126, 137, komabe zikuoneka kuti Masalimo analembedwa osapitirira chaka cha 500 B.C.[25]

Mutu ndi Cholinga: Cholinga cha Masalimo ndi kupereka mawu a chitonthozo ndi chilimbikitso, kudzera mu mapembezero, mmapemphero ndi chiyamiko. Mu Masalimo tikuonanso mtima wa Mulungu, zomwe munthu amakumana nazo pamoyo, ndi thandizo lomwe Mulungu amapereka pa anthu.

Ngakhale mabukhu a Masalimo ali ambiri ndi mitu yosiyana siyana, koma zoona ndi zakuti, bukhuli likupereka chiyembekezo pa anthu okhulupilira Mulungu, kuti adzalanditsidwa kwa adani, kuthandizidwa ndi kukumbukiridwa, nthawi zones. Masalimo 2, akukamba za malingaliro a Mulungu, kuti ndi apadera-dera, oposa a munthu.[26]

Masalimo ambiri akunena za Mesiya, ndi Mulungu atate.

Zigawo za Bukhu la Masalimo: Masalimo anagawidwa zigawo zisanu, ndipo gawo lirilonse limatsiriza ndi matamando kwa Mulungu, ndipo potsiriza pa zones, Masalimo 150 akutsendera matamando pa mabukhu onsewa.

Ephanius anati, “Ahebri anagawa bukhu la Masalimo, mu zigawo zisanu, iwo amafuna apange Pentateuch wina, Midrasi wa Masalimo 1:1 anati: Mose anapereka kwa iwo bukhu la Masalimo mu magawo asanu.[27]

Zigawo za Mabukhu asanu a Masalimo ali motere:[28]

1. Salimo la munthu ndi chilengedwe (1–41) Lifanana ndi Genesis
2. Salimo la chiombolo cha Israeli (42–72) Lifanana ndi Eksodo
3. Salimo la mapembezero ndi Kachisi (73–89) Lifanana ndi Levitiko
4. Salimo la Kukhala kwathu mudziko (90–106) Lifanana ndi Numeri
5. Salimo la Matamando ndi awu a ulungu (107–150) Lifanana ndi Deuteronomu

Bukhu	Salimo	Mlembi	Zolembedwamo
I	Masalimo 1–41	Davide	Nyimbo ya matamando
II	Masalimo 42–72	Davide & Korah	Nyimbo yopempha
III	Masalimo 73–89	Asaphi	Nyimbo yopempha
IV	Masalimo 90–106	Wosadziwika	Nyimbo yokweza Yehova
V	Masalimo 107–150	Davide ndi Wosadziwika	Nyimbo yokweza Yehova

Mitundu ya Masalimo: Monga magawo awa

1. **Chisoni/kulira/kupempha:** Kulira kwa munthu mmodzi (Masalimo 3), kapena gulu la wanthu (Masalimo 44)
2. **Chithokozo/matamando:** munthu payekha (Masalimo 30), gulu la anthu (Masalimo 65)
3. **Kudalira/ kukhulupilira:** (Masalimo 4)
4. **Kumukweza pampando wachifumu wa YAHWEH:** Salimo lokhuza Yerusalemu (Masalimo 48), Masalimo a mesiya (2, 110)
5. **Chiphunzitso ndi nzeru:** (Masalimo 1, 37, 119)
6. **Masalimo okhuza nkhani yina yake:** A chilengedwe (8, 19), a zolengedwa (19, 104), a zida (111, 112, 119), a ulendo/eksodo (78), a kulapa (6), a kupemphera pa malo oyera (120), a mesiya (2, 8, 16, 22, 40, 45, 72, 110, 118)

Anthu: Bukhuli, ngakhale latchulapo Davide, Korah ndi ena, likukamba kwambiri za pfuko la anthu osati munthu payekha.

Khristu mu Nkhaniyi: Masalimo ambiri ndi a Mesiya ndipo akusonyeza Khristu ndi ntchito yake ndipo ali mu magawo awa:

1. **Zokhudza Mesiya mwachindunji:** Mabukhu ake ndi awa (Masalimo 34:20; 69:4, 9) koma nkhani zambiri zikulongosola. Mwina malinga ndi nkhani iyi, Yesu ndi Atumwi analongosola bwinonso za Masalimo (Masalimo 109:8 ndi Machitidwe 1:20).
2. **Mauneneri:** Ngakhale masalimo amazilongosolanso okha, apa amalongosolanso za umunthu wa Khristu. Uneneri wa Khristu (Masalimo 22)
3. **Zokhudza Mesiya mwachining'a:** amanena kuti, nyumba ya Davide, polongosola za Mesiya (Masalimo 2, 45 ,72)
4. **Uneneri woonekeratu:** Awa ndi Masalimo omwe Khristu amanena ochitira umboni za Khristu mwana wa Davide (Masalimo 110)
5. **Kukweza pa mpando wachifumu:** Masalimo onena za kukwezedwa kwa Khristu pa mpando wachifumu wa Mulungu (96-99)

Mauneneri awa Akwaniritsidwa kwa Khristu:

Uneneri	Masalimo	Nkhani ya M'chipangano Chatsopano
1. Kubadwa	104:4	Ahebri 1:7
2. Kuzichepetsa	8:4	Ahebri 2:6
3. Umulungu	45:6	Ahebri 1:8
4. Utumiki	69:9	Yohane 2:17
5. Kukanidwa	118:22	Mateyu 21:42
6. Kuperekedwa	41:9	Yohane 13:18
7. Kupachikidwa	22	Mateyu 7:39, 43, 46; Luka 23:35
8. Kuuka Mmanda	2 And 16	Machitidwe 2:27
9. Kukwera Kumwamba	68:18	Ephesians 4:8
10. Kulamulira	102:26	Ahebri 1:11

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Bukhu I: Nyimbo Zopembezera (Masalimo 1–41)**
   Masalimo 1: Munthu wodala: Njira ziwiri zotsutsana pa moyo, Mawu ndi Za mdziko
   Masalimo 2: Mesiya ndi mfumu
   Masalimo 3: Chitetezo ku zoopsa
   Masalimo 4: Pemphero la madzulo, kudalira pa Mulungu
   Masalimo 5: Pemphero la mmawa
   Masalimo 6: Pemphero la muuzimu
   Masalimo 7: Pemphero la mpumiro
   Masalimo 8: Ulemerero kwa mulengi
   Masalimo 9: Pemphero lothokoza Mulungu pa chilungamo chake
   Masalimo 10: Pemphero logonjetsera choipa
   Masalimo 11: Yehova, pothawirapo ndi chitetezo chathu
   Masalimo 12: Pemphero kwa Mulungu, kukana lirime labodza
   Masalimo 13: Pemphero pa mavuto
   Masalimo 14: Kuposa kwa munthu wochimwa
   Masalimo 15: Kulongosola munthu woopa Mulungu
   Masalimo 16: Yehova ndiye pothawirapo okhulupilira
   Masalimo 17: Pemphero la chiwombolo
   Masalimo 18: Pemphero ndi pembezero la chiwombolo
   Masalimo 19: Mavumbulutso a Mulungu pa chilengedwe, ntchito ndi mawu olembedwa
   Masalimo 20: Kupempherera chigonjetso pamaso pa adani
   Masalimo 21: Yehova, monga mphamvu yamafumu
   Masalimo 22: Chidzindikiro cha mtanda: Salimo la matamando
   Masalimo 23: Salimo la Mulungu wabwino
   Masalimo 24: Salimo la mfumu ya Ulemerero
   Masalimo 25: Pemphero la chiombolo, chitsogozo ndi kukhulukira machimo
   Masalimo 26: Kupempherera chiyero ndi chiwombolo
   Masalimo 27: Kupemphera mopanda mantha
   Masalimo 28: Kupempha thandizo–Yehova ndiye Thanthwe lathu
   Masalimo 29: Mawu a mphamvu a Mulungu
   Masalimo 30: Pemphero lakuthokoza Mulungu mu nthawi ya mavuto
   Masalimo 31: Pemphero la dandaulo, matamando ndi kumukweza
   Masalimo 32: Madalitso a kukhululukidwa, ndi kukhulupilira Mulungu
   Masalimo 33: Matamando kwa Mulungu wopereka ndi woombola
   Masalimo 34: Matamando kwa Mulungu wopereka ndi woombola
   Masalimo 35: Pemphero la chilungamo ndi chitetezo kwa adani
   Masalimo 36: Kuchimwa kwa munthu, poyerekeza ndi chifundo cha munthu.
   Masalimo 37: Kupempha mpumulo mwa Mulungu
   Masalimo 38: Pemphero lakuvomereza ndi kubrerezedwanso
   Masalimo 39: Pemphero lovomereza kuchimwa kwa munthu
   Masalimo 40: Matamando pa chimwemwe ndi chipulumutso
   Masalimo 41: Matamando kwa Mulungu chifukwa chopambanitsa pa zipsinjo

2. **Bukhu II: Nyimbo za Kupempha (Masalimo 42–72)**
   Masalimo 42–43: Kukhala pa Mulungu, kulindira Ambuye
   Masalimo 44: Pemphero la chiombolo cha dziko
   Masalimo 45: Nyimbo ya ukwati wa mwana wa Davide
   Masalimo 46: Mulungu, pothawira ndi pobisala pathu
   Masalimo 47: Mulungu, mfumu yachigonjetso
   Masalimo 48: Ziyoni, mzinda wokongola
   Masalimo 49: Chuma chopanda nzeru chiri chabe
   Masalimo 50: Nsembe yachithokozo
   Masalimo 51: Kuvomereza machismo, kupempha chikhululukiro
   Masalimo 52: Kuzikuuza kwa oipa kuli chabe
   Masalimo 53: Opanda Mulungu
   Masalimo 54: Yehova, thandizo lathu
   Masalimo 55: Yehova, thandizo la omukhulupilira
   Masalimo 56: Kudalira Mulungu panthawi ya zoopsa
   Masalimo 57: Kumkweza Yehova
   Masalimo 58: Dipo kwa olungama
   Masalimo 59: Pemphero la chiombolo pamaso pa adani

Masalimo 60: Pemphero la chiombolo cha dziko
Masalimo 61: Pemphero la mtima wopsinjika
Masalimo 62: Kulindira pa Yehova
Masalimo 63: Ludzu la chikondi cha mulunguo
Masalimo 64: Pemphero la chitetezo
Masalimo 65: Dziko ndi Munthu
Masalimo 66: Kukumbukira zomwe Mulungu wachita
Masalimo 67: Onse apembedze Mulungu
Masalimo 68: Yehova, Tate wa opsinjika
Masalimo 69: Pemphero la chiombolo, chisoni cha Mulungu
Masalimo 70: Pemphero la osowa ndi amasiye
Masalimo 71: Pemphero la okalamba
Masalimo 72: Ulemelero wa ufumu wa Mesiya

3. Bukhu III: Nyimbo Zopemmpha (Masalimo 73–89)
Masalimo 73: Pephero la mkati mwa mtima
Masalimo 74: Pemphero lopempherera dziko, nthawi ya mavuto
Masalimo 75: chilungamo ndi cha Yehova
Masalimo 76: ulungu wa Yakobo, wamphamvu ndi wogonjetsa
Masalimo 77: Mu nthawi yamavuto
Masalimo 78: Phunziro pa mbiri ya
Masalimo 79: Mulungu akumbukire nkhosa pamsipu pake
Masalimo 80: Kupempherera chifundo cha Mulungu pa Israeli
Masalimo 81: Israeli amvere pa Mulungu
Masalimo 82: Osalungamma aweruzidwa
Masalimo 83: Chilango pa adani a Israeli
Masalimo 84: Kupezeka kwa Mulungu
Masalimo 85: Phunziro la chitsimutso
Masalimo 86: Phunziro la zifundo za Mulungu pa pfuko
Masalimo 87: Chimwemwe pakukhala mu ziyoni
Masalimo 88: Pemphero mu mdima ndi mu zipsinjo
Masalimo 89: Kulindira pa Mulungu

4. Bukhu IV: Nyimbo za Matamando (Masalimo 90–106)
Masalimo 90: Kuwerengera masiku
Masalimo 91: Mu nthunzi wa wamwambamwambayo
Masalimo 92: Mulungu alemekezeke
Masalimo 93: YAHWEH muulemelero wake
Masalimo 94: YAHWEH woweruza dziko lapansi
Masalimo 95: Kugwadira Yehova
Masalimo 96: Pembedzani Mulungu
Masalimo 97: Kondwerani
Masalimo 98: Imbani nyimbo yatsopano kwa Mulungu
Masalimo 99: Mukwezeni Mulungu
Masalimo 100: Tumikirani Yehova mwachimwemwe
Masalimo 101: Kudzipereka ku moyo wachiyero
Masalimo 102: Pemphero la wolungama
Masalimo 103: Chifundo cha Mulungu
Masalimo 104: Mulungu asamalira zolengedwa zonse
Masalimo 105: Kukhulupirika kwa Mulungu
Masalimo 106: Kukumbukira chikondi cha Yahweh pa Israeli

5. Bukhu V: Nyimbo zamatamando (Masalimo 107–150)
Masalimo 107: Matamando pa chiombolo cha Yehova
Masalimo 108: Pemphero la chipambana
Masalimo 109: Pemphero la chigonjetso pa adani
Masalimo 110: Mesiya monga wansembe, mfumu ndi wankhondo
Masalimo 111: Kukondwerera kukhulupilika kwa Mulungu
Masalimo 112: Chimwemwe cha chikhulupiliro
Masalimo 113: Kutamanda Yehova
Masalimo 114: Kuthokoza
Masalimo 115: Mafano alibe Moyo, Mulungu ndiye wamoyo
Masalimo 116: Kutamanda Mulungu pa chiwombolo

Masalimo 117: Kutamanda kwa anthu onse
Masalimo 118: Kutamanda Yehova
Masalimo 119: Kulemekeza malemba
Masalimo 120: Pemphero la chiwombolo
Masalimo 121: Yehova, mtetezi wathu
Masalimo 122: Kupempherera mtendere ku Yerusalemu
Masalimo 123: Kupempha chifundo
Masalimo 124: Wothandiza ndi wolenga zonse
Masalimo 125: Mtendere mu Israeli
Masalimo 126: Matamando pa kubwezeretsa
Masalimo 127: Pembezero chifukwa cha ana, mphatso yochokera kwa Mulungu
Masalimo 128: Banja lodalitsidwa
Masalimo 129: Pemphero la ozunzidwa
Masalimo 130: Kulindira chiombolo chake
Masalimo 131: Khulupilirani mwa Yehova
Masalimo 132: Dalitso la Mulungu pa Ziyoni
Masalimo 133: Kudalitsidwa mu umodzi
Masalimo 134: Pemphero, madzulo
Masalimo 135: Kuthokoza Mulungu
Masalimo 136: Chifundo chake ndi chosatha
Masalimo 137: Misonzi mu ukapolo
Masalimo 138: Mulungu amayankha ozichepetsa
Masalimo 139: Mulungu amatidziwa
Masalimo 140: Pemphero la chiwombolo
Masalimo 141: Pemphero likhale ngati zonunkhiritsa
Masalimo 142: Mulungu, yekhayo wotisamala
Masalimo 143: Pemphero la chitsogozo
Masalimo 144: Yehova, Thanthwe lathu
Masalimo 145: Ntchito zozizwitsa za Mulungu
Masalimo 146: Mulungu, Mthandizi wathu
Masalimo 147: Mulungu, wochiza mitima yosweka
Masalimo 148: Mulungu, mlengi wa nzeru
Masalimo 149: Mulunguwokondwera ndi anthu ake
Masalimo 150: Matamando kwa Mulungu

Miyambo

(Nzeru kuchokera kwa Mulungu)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Malinga ndi 1 Mafumu 4:32, Solomo anayankhula pa anthu miyambi/ Miyambo 3,000, ndi nyimbo 1,005 ndipo mabukhu omalizira akusonyeza kuti Solomo ndiye mlembi wa bukhu la Miyambo (Miyambo 1:1–9:8; 10:1–22:16; 25:1–29:27). Komabe Miyambo ina (25:1–29-27) inasankhidwa pa zoyankhula za Solomo, mosankhidwa ndi komiti ya Hezekiya (25:1), Miyambo 22:17 imati “zonena za mwini nzeru,” ndipo 24:23 akunena chimodzimodzi. Miyambo 22:17-21 ikupereka chithunzi cha gulu la anthu anzeru, osati Solomo yekha. Ndipo mutu 30 ukunena za Aguri, mwana wa Jakeh, ndipo 31:1-9 akunena za Lemueli.

Bukhu la Miyambo linapeza dzina lake kuchokera mu zolembedwazi–miyambi ndi zolankhulidwa zina monga malangizo zomwe zimafika mwachindunji pokamba choonadi. Mawu a chiHebri okamba za miyambo amatanthauza “zifanifani”, “mafanizo” kapena zinthu zoti zikufananizidwa ndi zina. Izi zonse zimafananizidwa ndi zinthu zimene zimachitika pa moyo wa munthu komanso zimapereka maphunziro a m’moyo uno. Miyambo siimangolunjika pofananiza zinthu kokha ndi zinthu zina komanso ndi zinthu zina zimene ziri zosiyana.

Bukhuli linatenga dzina lake kuchokera pa malangiza a Miyambo okhudza chikhalidwe ndi moyo wa uzimu zimene zimathandiza munthu kuti akhale wanzeru.

Zaka: 950–700 B.C. Miyambo ndi bukhu la mbiri komanso lophunzitsa za nzeru ndi kuopa Yehova. Miyambo ya Solomo inalembedwa mu zaka za 931 B.C., ndipo miyambo ina anatoleredwa ndi Hezekiya mu zaka za 700 B.C.

Mutu ndi Cholinga: Cholinga cha bukhuli ndi kupereka mwambo, kulangiza ndi kuphunzitsa anthu kuti akhulupilire Mulungu, akhale moyo wabwino mdziko, moyo wabwino kwa anzake. Bukhuli limakambanso za ulesi, kugwira ntchito, lilime kunyada, chigololo, kuba, kupha, kupatsa, kumana, kulanda, umboni, abale, chikondi, mazunzo, ubwino, chuma, tchimo, ndi moyo, choonadi ndi banja, ndi zina zambiri za pa moyo wa munthu. Ndipo palibenso bukhu lina mu Baibulo, lomwe lalongosola kwambiri motere.

Mutu weniweni wa bukhuli ndi: ***"Chiyambi cha nzeru ndiko kuopa Mulungu"*** (Miyambo 1:7), kuopa Mulungu ndi kumudalira mu zones ndi nzeru ndipo munthu wotere amadalitsidwa ndi kuomboledwa ndi Mulungu (2:1-5).

Anthu mu Bukhuli: Bukhuli lalembedwa kwa wina aliyense, choncho palibe munthu yemwe wanenedwa mu nkhaniyi, monga mwini nkhani.

Khristu mu Nkhaniyi: Mu chaputala 8, nzeru zikuonedwa ngati munthu mu chiyeretso chake. Ndi woyeretsedwa (8:22-31), phata lake ku thupi ndi kuuzimu (3:18; 8:35-36), ndi wolungama (8:8-9), ndipo wopezeka kwa aliyense womulandira iye (8:1-6, 32-35). Nzeru inakhala ngati thupi, Yesu Khristu, ***"mwa iye mowe muli Chuma Chobisika Cha Nzeru ndi Chidziwitso"*** (Akolose 2:3), ***"koma mwa iye inu muli mwa Khristu Yesu yemwe anali nzeru yochokera kwa Mulungu ndi Chilungamo ndi Chiyero ndi Chiombolo"*** (1 Akorinto 1:30; 1 Akorinto 1:22-24).[29]

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Chiyambi: Cholinga cha Miyambo (1:1-7)**

2. **Mawu a Nzeru: Miyambo kwa Achinyamata (1:8–9:18)**
   a. Kumvera makolo (1:8-9)
   b. Kusayenda ndi anthu oyipa (1:10-19)
   c. Kumvera malangizo ndi mawu a nzeru (1:20-33)
   d. Kusachita chigololo (2:1-22)
   e. Kukhulupilira ndi kulemekeza Mulungu (3:1-12)
   f. Madalitso a nzeru (3:13-20)
   g. Kukhala achifundo kwa ena (3:21-35)
   h. Kupeza nzeru (4:1-9)
   i. Kukana mabwalo a onyoza (4:10-19)
   j. Koposa zonse sunga mtima wako (4:20-27)
   k. Usachite chigololo (5:1-14)
   l. Ukhale wokhulupilika kwa okondedwa wako (5:15-23)
   m. Uzipewa chikole (6:1-5)
   n. Usakhale waulesi (6:6-19)
   o. Chigololo ayi (6:20-35)
   p. Pewa mkazi wa chigololo (7:1-27)
   q. Nzeru ndi kupusa zikumana (8:1-9:18)

3. **Miyambo ya Solomo (10:1–24:34)**
   a. Miyambo yofanizira ochimwa ndi oopa Mulungu (10:1–15:33)
   b. Miyambo yolimbikitsa moyo wa uzimu (16:1-22:6)
   c. Miyambo yosonyeza zochitika zosiyanasiyana (22:17–23:35)
   d. Miyambo yokhudzana ndi anthu osiyanasiyana (24:1-34)

4. **Miyambo ya Mfumu Solomo Yomwe Inatengeredwa pa Otsatira a Hezekiya (25:1–29:27)**
   a. Miyambo yokhuza maubale ndi ena (25:1–26:28)
   b. Miyambo yokhuza zochitika (27:1–29:27)

5. **Mawu a Aguri (30:1-33)**
   a. Mawu a iye mwini (30:1-14)
   b. Miyambo ya chiwerengero (30:15-33)

6. **Mawu a Lemueli (31:1-9)**

7. **Mkazi wa Ngwiro (31:10-31)**

Mlaliki

(Chilungamo Kudzera mu Choonadi)

Mlembi ndi Dzina la Bukhuli: Pali milozo iwiri ya Chitsindikizo (wakunja ndi wamukati) imene imalozera kuti solom ndiye adalemba buku la Mlaliki. Mulozo wakunja imatsimikiza kuti miyambo ya ChiYuda imapereka bukuli kwa Solomo kuti ndiye mlembi wake. Mulozo wamkati, malo uchuluka akuliwonetsera ndi chisimikizo chonse kuti Solomo ndiye adalemba bukuli choyamba, olemba akuzionetsera yekha kuti ndi ***"Mwana wa Davide, Mfumu ya ku Yeresalemu"*** (1:1). Kenaka, mau ena aumboni mamabuku amene, Mlembiyu adaonetsa

kupambana kwa nzeru yake (1.16), Kuchulukitsa kwa chuma chake (2:7), Mwai wa zisangalalo (2:3) ndi maluso a zomangamanga (2:4-6). Znsezi zimapereka lingaliro lakuti Solomo ndiye adalemba bukhuli.
Mwachindunji, palibe aliyense ochokera ku pfuko la Davide amene angafanane ndi zimene zalembedwa ndi kufotokozeredwa.

Dzina lakuti Mlaliki limachokera ku mutu woperekedwa mu Chigiriki. Dzinali limatanthauza msonkhano, mawu a muchihebri/Yuda amatanthauza kuyankhula ndi kutsogolera pa "Msonkhono" kapena "Mulaliki."

Zaka: 931 B.C. Kolingana ndi chikhalidwe cha chiYuda, Solomo analemba nyimbo ya Solomo mu zaka zake zoyambirira kufotokoza chikondi cha munthu wachichepere. Analembanso bkuu la miyambo ku ukulu wake, kuwonjezera nzeru za munthu wakutha msikhu, analemba Mlaliki zaka za kumapeto kuukulu, kudandaula kwa munthu wokalamba. Mwanjira ina Mulaliki ndi mawu osungidwa, osonyeza kudandaula, kulapa, komanso kukumbukira, ku zofooka (zolakwitsa) zake zolembedwa mu 1 Mafumu 11. Bukhu la Mlaliki liyenera kuti limalembedwa Solomo atasala pang'ono kumwalira komanso ufumu wake utatsala pang'omo kuti ugawikane zidachitika 931 B.C.[30]

Mutu ndi Cholinga: Mutu wa bukhuli ndi kutsimikizira za moyo pambali pa kukhala ndi Mulungu; pamene tikupitabe ndi bukhuli, tipezanso mitu ina ndi zolinga zenizeni zinai, zoonekera.

Choyamba, pakufuna kuonetsera kuti moyo wopanda Mulungu ulibe tanthauzo, Solomo akufuna kuchotsa chitsimikizo cha kuika chikhulupiliro pa zimene iye wapindula mu moyo uno ndi nzeru akuwonetsa kuti zones zimene munthu akufuna azafike kumapeto kwake, kapena njira imene imaoneka yabwino kwa munthu, chachidziwikire idzaoneka yosakhutsa mtima. Solomo analemba kusakhutira ndi kupanda kanthu kwake, kuti apereke chidwi kwa owerenga kuti iwo akhale ndi njala ya Mulungu. Amafuna kuonetsa kuti zokhumba za munthu sizikondweretsa kapena kukhutitsa mtima.

Chachiwiri, Solomo anatsimikizira kuti moyo ndiovuta kuumvetsa, zimene zikutiphunzitsa kuti tiyenera kukhala ndi moyo ndi chikhulupiliro, osakhala pa zomwe tikuziona ayi, moyo ndi wodzala ndi zinthu zovuta kulongosola. Pali zambiri mu moyo zomwe munthu sangalongosole, kapena kuzimvetsa. Koma mwa chikhulupiliro, tikhoza kukhala mu nzeru yopambana, ndi ntchito ya Mulungu. Monga zalembedwa zochuruka mu bukhu la Yobu, sizingotsimikizira kokha kuti munthu ali ndi malire, koma kuti aphunzirenso kukhala ozindikira munzinsinsi. Moyo pa dziko lino, sungathe kubweretsa pawokha mayankho a moyo uno. Poonetsetsa izi; munthu ayenera kukhala ndi maonekedwe oposa mmene dziko limamuonera. Ayenera ayang'ane kwa Mulungu, kukhulupilira ndi kudalira iye.

Chachitatu, Mlaliki amationetsera maonekedwe enieni a moyo mosiyana ndi bukhu la miyambo, limaonetsa kuti moyo ndi olekana ndi zofunika za miyimbo (Miyambo 10:16) imatsimikiza kuti chilungamo ndi cholungama ndi oipa omwe. Koma Mlaliki 8:14 amaonetsa kuti nthawi zones izi sizizakhala choncho, makamaka mmoyo uno.Kodi uku ndi kutsutsana? Ayi, Chifukwa miyambo ikuonetsa mfundo zokhazikika za Mulungu osaonetsapo zolephera zimene zimapezeka pokhala mdziko lochimwa. Mlaliki akuonetsa kuti,ngakhale pali ndondomeko za choonadi, monga kwalembedwa ku miyambo, sidzakhala chitsimikizo nthawi zones kwa munthu, mmene awonera zinthu, chifukwa munthe ali ndi malire.

Chachinayi, kuonetsa kuti, akasiyidwa kuti atsate ndondomeko za iye yekha, azapeza kuti palibe kanthu kalikonse mu moyo, kudzala ndi kukhumudwa. Ngakhale ziri chncho, izi sizisonyeza kuti moyo ndi wopanda ntchito, komanso wopanda tanthauzo. Tanthauzo ndi kufunikira zikhoza kupezeka makamaka mukumuwopa Mulungu, zokhumudwitsa zingathe kuchepetsedwa polola kuti moyo ukhutitsidwe ndi kuyanjana ndi Mulungu.

Anthu Ofunika: Mfumu Solomo

Khristu mu Bukhuli: Pokhala kuti Khristu ndiye njira yokhayo ya munthu, kuti apeze Mulungu kumene munthu amapeza kukhutitsidwa, kapena moyo ochuruka (Yohane 10:10; 7:37-38), kusakwaniritsidwa mu moyo kudzachoka pokhapokha ngati pali ubale wabwino pakati pa munthu ndi Yesu Khristu. Kufunitsitsa kwa munthu kuti akhale wokhutitsidwa, zimapezeka mwa Khristu, Mpulumutsi yekha.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Malonje; Vuto Litchulidwa (1:1-3)**

2. **Vuto Liwonetseledwa (1:4–2:26)**
   a. Moyo (1:4-11)
   b. Nzeru za munthu (1:12-18)
   c. Chuma (2:1-11)

d. Kuzikundikira zinthu (2:12-23)
e. Mathero (2:24-26)

3. **Dongosolo la Mulungu (3:1-22)**
   a. Anakhatsikilatu zochitika pa Moyo (3:1-11)
   b. Anakhazukiratu mfundo pa Moyo (3:12-13)
   c. Mulungu aawerua onse (3:14-21)
   d. Mathero (3:22)

4. **Malonje (4:1–5:20)**
   a. Kupondeleza (4:1-3)
   b. Kugwira Ntchito (4:4-12)
   c. Tsogolo la ndale (4:13-16)
   d. Chipembezo (5:1-7)
   e. Chuma chapadziko chachabe (5:8-17)
   f. Mathero (5:18-20)

5. **Moyo (6:1-12)**
   a. hua sikwana (6:1-2)
   b. Ana sakhutitsa (6:3-6)
   c. Nthito sikhutitsa (7-12)

6. **Langizo (7:1–12:8)**
   a. Langizo la kuipa Kwa Munthu (7:1-29)
   b. Langizo pa Mphaso la Mulungu (8:1–9:18)
   c. Langizo pa Moyo (10:1-20)
   d. Langizo pa ukalamba (11:1–12:8)

7. **Mathero (12:9-14)**

Nyimbo ya Solomo

(Chimwemwe mu Umodzi)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Solomo akutchulidwa kasanu ndi kawiri (1:1-5; 3:7, 9, 11; 8:11-12), ndipo akuonetsedwa ngati mkwati. Ndime yoyambirira imaonetsera kuti, Solomo analemba bukhuli monga imodzi mwa nyimbo zambiri zimene iye analemba (1 Mafumu 4:32) amatiuza kuti adapeka nyimbo 1,005 zonga izi. Mthengawu sukungonena kuti "Nyimbo ya Solomo" Koma kuti Nyimno mu Nyimbo zambiri zomwe Solomo adalemba.

Dr. Charles Ryrie adalemba kuti:

> Bukhu ili lapatsidwa mitu yambiri. Mutu wa chiHebri kuchokera vesi 1, nyimbo ya nyimbo imene imatanthauza 'yokongola.' Kapena 'yapamwamba' Mutu wachingerezi kuchokera mu vesi 1 nyimbo ya Solomo, imene inafotokozera za olemba, mauwa ndi ochokera ku chilatini.[31]

Zaka: Pafupifupi **965 B.C.**

Mutu ndi Cholinga: Nyimbo ya Solomo, ndi nyimbo ya chikondi yodzadzidwa ndi zithunzi za mawu kuonetsa chikondi cha mbanja, kukongola kwa chikondi chathupi pakati pa mwamuna ndi mkazi. Bukhuli likuimilira ngati sewero lokhala ndi magawo ambiri amene akuonetsedwa mmusimu.

Bukhuli linalembedwa masiku oyambirira a luso la Solomo. Pafupifupi 965 B.C., Nthawi imeneyi Solomo anali ndi mafumukazi makumi asanu ndi limodzi (60), kuzanso azakazi makumi asanu ndi atatu (80) (6:8). Koma kenakamuufumu wake, anali ndi akazi mazana asanu ndi awiri (700) kudzakazi mazana atatu (300) (1 Mafumu 11:3).

Anthu Ofunika: Mkwati (Shulamite), mfumu Solomo, atsikana a ku Yerusalemu

Khristu mu Nyimbo ya Solomo: Nyimbo ya Solomo imaonetsera chikondi cha Khristu kwa okhulupilira.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Mutu (1:1)**

2. **Kugwa Muchikondi (1:2–3:5)**
   a. Mkwati (1:1-8)
   b. Kukambirana za Chikondanao chawo (1:9–2:7)
   c. Mfumu ayendera ku nyumba ya mkwati (2:8-17)
   d. Loto la mkwati pakusiyana (3:1-5)

3. **Kugwirizana pachikondi (1–5:1)**
   a. Mwambo waukwati (3:6-11)
   b. Alemekeza kungola (4:1-15)
   c. Ukwati wa theka (4:16–5:1)

4. **Zochitika muchikondi (5:2–7:10)**
   a. Alekana nthawi (5:2-7)
   b. Alemekeza kungola kwamkwati (5:8–6:3)
   c. Alemekeza kungol kwamkwatibwi 6:4–7:10)

5. **Kunkhwima muchikondi (7:11–8:14)**
   a. Mkwatimbi akhumba kukachezera mkwati (7:11–8:4)
   b. Mkwatimbi abwelera kwawo (8:5-14)

Gawo 4
Mabukhu a Aneneri Aakulu

Malonje: Mu kauniuni wa chipangano chakale, taonanso “mabukhu a chilamulo,” “mabukhu a mbiri,” ndi “mabukhu a ndakatulo” ndipo palinso gawo lomaliza la “mabukhu a auneneri.”

Mabukhu a aneneri ang “ono-ang” ono khumi ndi awiri ndi awa: Aneneri awa, amadziwikanso kuti Aneneri olemba, chifukwa amalemba ndi kusunga mawuwo:

Aneneri agawidwa motere: Aneneri aakulu ndi Aneneri Aang’ono. Aneneri akuluakulu ndi awa: Yesaya, Yeremiya, Maliro, Ezkieli ndi Danieli. Mabukhu 12 a aneneri aang’ono ndi awa: Hoseya, Yoweri, Amosi, Obadiya, Yona, Mika, Nahumu, Habakuku, Haggai, Zekariya ndi Malaki.

Aneneri osalemba omwe sanasiye mbiri yolembedwa ya uneneri wawo ndi awa: Natani, Ahija, Shemiya, Jahaziel ndi Hilda.

Alembi: Olemba mabukhu a uneneri amatchulidwa ndi maina osiyanasiyana monga: Aneneri, Oyang’anira, Alonda, Anthu a Mulungu, Otumikira, Akapolo a Ambue.

Mau oti Mneneri, akutanthauza kuti “wolankhulira, kapena wonenera mmalo mwa wina.” Choncho mmeneri amalankhula mmalo mwa Mulungu, kwa anthu. Izi zalongosoledwa bwino mu ndime zitatu, motere: (1) Eksodo 6:28–7:2. Pamene Mosee anakana kukhala wolankhulira Mulungu kwa Farao, Nulungu anasankha Aaroni kuti akhale Mneneri wa Mose. (2) Numeri 12:1-8 Aaroni ndi Miriyamu, chifukwa cha kaduka, anafuna kutenga malo a Mose a unkhalapakati pa bvumbulutso la ulungu ndi anthu, koma Mulungu adalowelera modabwitsa kuti awonetse kuti woyenera kulankhula mwachindunji ndi mose yekha, komanso ngati angathe kulankhula kudzera mwa okha otchedwa Aneneri. (3) Deutronomu 18:9-22, atalongosola pang’ono za imfa ya Mose, tiri kudziwitsidwa chiyambi cha utumiki wa uneneri, ndipo malemba akupitilira kunena kutiamayankhula mwachindunji uthenga, umene Mulungu wamuululira iye.[32] Ntchito ya mneneri inali yolankhulira Mulungu, kulalikira nkhani zimene Mulungu wanena, zomwe zichitike lero, msangasanga, mawa, mtsogolo.

Aneneri Amagwira Ntchito Ngati: Uthenga: monga mnneneri wa Mulungu, aneneri ntchito yawo ndi yolankhula zomwe mulungu wawauza. Tanthauzo la uneneri ndi kulalikira za zinthu zomwe zikuchitika,kunenera za mtsogolo,komanso kunenera za zomwe mulungu wanena. Pali njira imodzi yodziwira unenera. Wonenerayo Amati “Atero Ambuye.”

Pali ndondomeko zitatu za uneneri mu chipangano chakale.

Choyamba, anagwira ntchito monga alaliki omwe anaphunzitsa ndi kumasulira Chilamulo cha Mose ku pfuko lonse. Komanso anali ndi ntchito yochenjeza, kudzudzula, kuweruza ndi kuitanira anthu mu kulapa (Yona 3:4).

Kachiwiri, amalengeza za chilango chirinkudza, chiombolo, ndi zochitika zokhudza Mesiya ndi ufumu wake. Kulosera za tsogolo pofuna kupereka chiyembekezo pa munthu, kuonetsera kuti Mulungu amadziwa komanso amawongolera tsogolo, ndipo amapereka mabvumbulutso aphindu. Ulosi wa Mnneneri weniweni, umadzakwaniritsidwa ndithu, sulephereka. Ulosi ukalepherka ndiye kuti mneneri ananenera zomwe Mulungu YAHWEH sanamuuza (Deuteronomu 18:20-22). 1 Samueli 3:19 zinanenedwa za Samueli kuti Ambuye anali naye.

Kachitatu, aneneri anagwira ntchito ya Ulonda wa Israeli (Ezekieli 3:17). Ezekieli anaima monga mlonda wa linga la Ziyoni, kuomba lipenga, kuchenjeza anthu za chilango pa kusamvera kwawo. Iye anawachenjeza anthuza kuyanjana kwawo ndi andale komanso asilikari ankhondo, mayesero, maufumu ena achilendo, ndi kupembeza.

Pomaliza, ngakhale aneneri anagwira ntchito mu njira zambiri monga momwe mulungu anawalamulira, iwowa anagwira ntchito ya ukazembe komanso wotanthauzira malamulo mu dziko la Israyeli ndi Pangano la pa Mose.[33]

Kusiyanisa Aneneri Akuku Akulu Anayi[34]

Kusiyanisa Aneneri Akuku Akulu Anayi				
	Yesaya	**Yeremiya**	**Ezekieli**	**Danieli**
Ananera kwa:	Ayuda mu Yudeya	Ayuda mu Yudeya ndi mukapolo	Ayuda mukapolo kubabulo	Ayuda kukapoplo kubabulo ndi mfum ya amitundu
Zokhuza:	Yuda ndi Yerusalemu (Yesaya 1:1; 2:1)	Yuda ndi Mafuko (Yeremiya 1:5, 9-10; 2:1-2)	Fuko lonse la Israeli (Ezekieli 2:3-6; 3:4-10, 17)	Israeli ndi amitundu (Danieli 2:36-43; 9)
Nthawiya ufumu wa:	Uzziya, Yotamu, Ahazi, Hezekiya (Mafumu Ayuda)	Yosiya Yooahazi, Yehoiakimu, Yehoyichini, Zedekiya (Mafumu a Yuda)	Zedekiy (Fumu ya Yuda); Nebukadinezera (Fumu ya Baibulo)	Yehoiakimu, Yehoiachini, Zedekiya (Mafumu a Yuda); Nebuchadinezra (Fumu ya Baibulo)
Zaka:	740–680 B.C.	627–585 B.C.	592–570 B.C.	605–536 B.C.
Mamabuku ambiri:	2 Mafumu 15-21; 2 Mbiri 26-30	2 Mafumu 22-25	Danieli 1-6	Danieli 1-6

Nkhani Mwachidule ya Chiyembekezo Chakubwera kwa Yesu mu Chipangano Chakale[35]

Kufikira pano, maphunziro athu awonetsa kuti chilamulo chidayala maziko a Yesu Khristu mwa chisankho (election) (Genesis), chiombolo (Eksodo), kuyeretsedwa (Levitiko), chitsogoza (Numeri), ndi chilangizo (Deuteronomu) cha mafuko a Isreali monga chitetezo cha mawu a Mulungu (Aroma 3:1) ndi ndondomeko za Mesiya (Genesis 12:1-3; Aroma 9:4-5).

Kukonzekera kopitilira kwa kubwera kwa Khristu kunaperekedwa mu mabukhu ambiri polipatsa pfukoli, malao a Israeli monga cholowa chawo. (Yoswa), kenako dzikoli linaponderezedwa ndi mafuko achikunja ndipo linali losakhulupirika. Komabe Mulungu, anadzutsa oweruza ndipo anapeza kukhulupirika mu dziko' (Rute). Kukhazikika kudaperekedwa ku dziko kudzera mwa mfumu Sauli (1 Samueli) ndipo linadzakhazikika ndi mfumu Davide (2 Samueli) ndipo linalemekezedwa pansi pa ufumu wa Solomo ndi ulamuliro wake (1 Mafumu 1:10) Izi zidatsatana ndi kugawanika kwa dzikoli (1 Mafumu 11:22) kupanga mitundu khumi ya kumpoto ndi mitundu iwiri ya kumwera ya Yuda ndi Benjamini. Mitundu yonseyi inavutika ndi kuchepetsedwa (2 Mbiri) kenaka, inatengedwa kuukapolo ndi Asuri ndi Baibulo, (2 Mafumu). Zotsatira zake, Kachisi adavutika ndikunyentchera (1 Mbiri) ndi chionongeko (2 Mbiri). Komabe kukhulupirika kwa Mulungu kumalonjezano ake kunakhala chikhalire ndipo kenako kunali kumanganso kwa Kachisi (Ezara) ndikubwezeretsedwa kwa otsalira (Nehemiya), motsagana ndi chitetezo cha Mulungu (Estere).

Mumabukhu a ndakatulo, nthawi zones munali kufunisitsa chauzimu cha Khristu malingana ndi maziko a umunthu oyalidwa muchilamulo komanso molumikizana kwa mabukhu ambiri.

Mabukhu a Uneneri, amayang; ana tsogolo amayang'ana chiyembekezo cha Khristu. Malingana ndi Geisler, Izi zikuchitika motere:

> Aneneri oyambirira (Hoseya, Yoweli, Amosi) akudikira kubwezeretsedwa kwa dziko lonse ndi Mesiya. Yesaya ndi Mika, akulosera chipulumutso cha dziko lonse, kudzera mu kubwera kwa Yesy Khristu. Obadiya, Yona, Nahumu, Habbakkuku, ndi Zefaniya, akuchenjeza za kuonongeka kwa mafukowa. Maliro, akudandaula Poona chionongeko cha ku dziko pa Anthu a Mulungu. Yeremiya akunenera kutsindikizidwa kwa pangano la Khristu. Ezekieli, akuyembekezera kubweretsedwa kwa chipembezo cha dziko, ndipo. Danieli akulosera kubwezeretsedwa kwa dziko kumbali ya ndale. Utatha ukapolo wa kubabulo uja, Haggai ndi Zakariya akuchenjeza anthu za kumanganso chipembezo chawo, ndipo Malaki, akunena za kubwezeretsedwa pa umunthu ndi chikhalidwe chawo, ***"pamene akudikira kudzanso kwachiwiri kwa dzuwa la chilungamo, limene lidzawala ndi kuchiritsa mmapiko ake"*** (Malaki 4:2).[36]

Yesaya

(Chipulumutso cha Yehova)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Monga likunenera mwachindunji, mlembi wa bukhuli ndi Yesaya, mwana wa Amozi, mutu wa banja lodziwika ndi lodabwitsa mu pfuko lachiYuda. Yesaya akuoneka kukhala opezeka mu mabukhu a mabwalo oweruza milandu achifumu ngakhale nthawi ya ulamuliro wa Ahazi. Iye anali ophunzira

odziwa bwino za kunja kwa maiko amene anakhala kwambiri ku Yerusalemu, amene amadziwika ndi maulemu ndipo anali mlangizi pa nkhani zakunja. Ngakhale Yesaya amatsogozedwa ndi Mulungu, nthawi zambiri amalandira chiopsezo chifukwa amatsutsa chiyanjano chirichonse cha mphamvu ya kunja (ngakhale Asuri kapena Aigupto). Monga mwa lonjezo la Mulungu mu Chaputala 6, maitanidwe a Yesaya anali oikika kuti alephereke pakuti anthu anasankha kuika chidaliro chawo pa zochitika zandale ndi chiyanjano cha anthu, kulekana ndi malonjezo a Mulungu.

Miyambo yakale imayerekeza kuti adaphedwa mu nthawi ya Manese, podulidwa pakati ndi mpeni (Ahebri 11:37), pokhala analemba infa ya Senakarebu, mu Yesaya 37:37-38, ndikoyenera kuyerekeza kuti Yesaya anakhala ndi moyo kufikira infa ya Senakeribu mu chaka cha 681 B.C.[37]

Dzina la Yesaya, linatengedwa ku dzina la mlembiyu, Dzina la chiyuda la mneneriyu limatanthauza "YAHWEH ndi chipulumutso," imene ndi ndemanga yabwino ya mutu ndi zolembedwa zones za mubukhumu.

Zaka: 740–680 B.C. Yesaya anali ndi utumiki nthawi yaitali moyandikana ndi mathero a utumiki wa Uzziah (790–739 B.C.), ndipo anapitilira kufikira ulamuliro wa Yutamu (739–731 B.C.), ndi Ahazi (731–715 B.C.) ndi Hezekiya (715–686 B.C.). Potengera nthawi ya ulamuliro wa amitundu, Yesaya anatumikira kuchokera nthawi ya Tiglath Pileser (745–727B.C.), kufikira nthawi ya Senakeribu (705–681B.C.), wa ku Asuri.

Mutu ndi Cholinga: Dzina la Yesaya likupereka mutu wa bukhuli "Chipulumutso ndi cha YAHWEH." Izi ndi zotsimikizika chifukwa mawu oti "chipulumutso" akuoneka malo makumi awiri ndi mphambu zisanu ndi limodzi (26) mu bukhu la Yesaya, komanso kasanu ndi kawiri, mu mabukhu onse a aneneri. Chifukwa cha ichi, Yesaya amatchedwa "mneneri wolalika" chifukwa amanena zambiri zokhudza chipulumutso ndi ntchito yakuombola ya Mesiya. Zambiri zanenedwa mu bukhuli, ndi zokudza munthu ndi ntchito ya Mesiya ndi ufumu wake, kuposa bukhu liri lonse mu chipangano chakale.

Mwanjira ina, Yesaya ndi bukhu lopatulika laling'ono limene liri ndi magawo 66 (66 chapters), pamene Baibulo liri ndi mabukhu 66 magawo oyamba 39 a bukhu la Yesaya amalumikizana ndi mabukhu 39 a chipangano chakale amene kwakukulu amafutokoza za kubwera kwa Mesiya. Magawo 27 otsirizira, amalekana ndi mabukhu 27 a chipangano chatsopano, chifukwa amalankhula kwambiri za Mesiya ndi ufumu wake monga kapolo wa Ambuye. Magawo 1-39 amalongosola za kufunikira kwa munthu kuti alandire chipulumutso, magawo 40-66 amaulula kuperekedwa kwa chipulumutso Mwa Mesiya ndi ufumu wake.

Anthu Ofunika: Yesaya mneneri ndiye munthu wofunika m'bukhumu, koma YAHWEH akuoneka monga wamphamvu wa Israyeli, ngati woyera wa Israyeli komanso ngati Ambuye Mulungu Wamakamu, izi ndizo zimene ziri zofunikira kwambiri mu bukhu la Yesaya.

Khristu mu Bukhuli: Palibe bukhu mu chipangano chakale limene limatulutsa chithunzi cha Khristu limene liri lomveka ndi lokwanira bwino loposa bukhu la Yesaya. Yesaya amaonetsera Mesiya mu ukulu wake wapamwamba (16:1f), kubadwa ndi umunthu (7-14; 9:6; 11:1), mu utumiki wake mwa nzimu (11:2f), muchikhalidwe chake mwa Mulungu (7:14'9:6), kuchokera kwake ku pfuko la Davide (11:1), ntchito yake yachipulumutso, chiombolo ngati Mlowa mmalo (53), utumiki wake monga kapolo wopulumusta (49-52).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Mauneneri Achidzudzulo ndi Chilango (1:1–39:8)**
   a. Muneneri ozuzula Yuda (1:1–12:6)
      1) Chizuzulo pa Yuda (1:1–5:30)

1:1-9	2:12-22	5:1-7
1:10-17	3:1-12	5:8-30
1:18-31	3:13-26	
2:1-11	4:1-6	

      2) Kutumidwa Kwa Muneneri (6:1-13)

6:1-7	6:8-13

      3) Kubwera Kwa Mesiya (7:1–12:6)

7:1-9	8:9-22	10:20-34
7:10-16	9:1-7	11:1-10
7:17-25	9:8-21	11:11-16
8:1-8	10:1-19	12:1-6

   b. Uneneri udzudzula amitundu (13:1–23:18)
      1) Wodzudzula Baibulo (13:1–14:23)

13:1-5	13:17-22
13:6-16	14:1-23

2) Wodzudzula Asuri/Nenevi (14:24-27)
3) Wodzudzula Afilisiti (14:28-32)
4) Wodzudzul Amoabu (15:1–16:14)
5) Wodzudzula Damasiko ndi mdzake Israeli (17:1-14)
6) Wodzudzula Ethiopia (Kutsi) (18:1-7)
7) Wodzudzula Aigupto (19:1–20:6)

19:1-10	19:11-25	20:1-6

8) Wodzudzula Aigupto (21:1-10)
9) Wodzudzula Edomu (21:11-12)
10) Wodzudzula Arabiya (21:13-17)
11) Wodzudzula Yerusalemu (22:1-25)
12) Wodzudzula Tulo (23:1-18)

c. Uneneri siku la Yehova (24:1–27:13)
1) Chilango (24:1-23)
2) Chimwemwe ndi Madalitso Muufumu (25:1–27:13)

25:1-12	26:11-21
26:1-10	27:1-13

d. Uneneri Udzudzula Israeli ndi Yuda (Madalitaso ndi Matembelero) (28:1–35:10)
1) Tsoka pa Samaria/ Efraimu (28:1-29)

28:1-13	28:14-29

2) Tsoka pa Yuda (29:1–31:9)

29:1-8	29:17-24	30:18-33
29:9-16	30:1-17	31:1-9

3) Ufumu wa Mesiya, Mfumu yolungama (32:1-20)

32:1-8	32:9-20

4) Tsola kwa Suri, wosakadza Yerusalemu (33:1-24)

33:1-12	33:13-24

5) Tsoka kwa Mafuko (34:1-17)
6) Kudza Kwa ufumu (35:1-10)

e. Uneneri kwa Sanakaribu (36:1–39:8)
1) Mfuwu yochekera kwa asuri (36:1-22)
2) Chowonadi chochekera kwa Mulungu (37:1-7)
3) Chiwopsezo chochekera kw Asuri (37:8-35)

37:8-13	37:14-20	37:21-35

4) Chikondwelero pa asuri (37:36-38)
5) Kudwala kwa Hezekiya ndi kuchilitsidwa kwake (8:1-22)
6) Kuputsa kwa Hezekiya (39:1-8)

2. Mauneneri otonthoza kapena olimbikitsa (40:1–66:24)

a. Mauneneri akuomboledwa kwa Israeli ndi ukulu wa Mulungu (40:1–48:22)

40:1-20	43:8-13	45:8-25
40:21-31	43:14-21	46:1-13
41:1-20	43:22-28	47:1-15
41:21-29	44:1-8	48:1-16
42:1-13	44:9-20	48:17-22
42:14-25	44:21-28	
43:1-7	45:1-7	

b. Mauneneri a Muomboli wa Israeli (49:1–57:21)

49:1-13	52:1-15	56:1-12
49:14-26	53:1-12	57:1-21
50:1-11	54:1-17	
51:1-23	55:1-13	

c. Mauneneri a tsogolo labwino (58:1–66:24)

58:1-12	61:1-11	65:1-16
58:13-14	62:1-12	65:17-25
59:1-8	63:1-6	66:1-2
59:9-21	63:7-14	66:3-9
60:1-14	63:15-19	66:10-24
60:15-22	64:1-12	

Yeremiya
(Machenjezo a Tchimo ndi Chilango Chake)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Monga Yesaya, bukhuli likuonetsa mwachindunji kuti wolemba wake ndi Yeremiya, mwana wa Hilikiya, wochoka ku pfuko la ansembe wa Anatoti, mu pfuko la Benjamini (1:1). Yeremiya analamulira uneneri wake kwa mlembi wake Baruchi. Yeremiya amatchedwa "mneneri wolira" (9:1; 13:17), kapena mneneri "waundekha" mwina chifukwa analamulidwa kuti asakwatire (16:2). Amatchedwanso "mneneri wonyalanyaza" (1:6). Koma wolalikira mokhulupirika, maweruzo a Mulungu ku ufumu wa kumwera, wa Ayuda, ngakhale kuti analandira chitsutso, kumenyedwa, ndi kumangidwa mu ndende (11:18-23; 12:6; 18:18; 20:1-3; 26:1-24; 37:11; 38:28).

Bukhuli limatenga dzina lake pa mlembi wake Yeremiya. Dzina la Yeremiya limatanthauza "YAHWEH amakhazikitsa."

Zaka: 627–585 B.C. Yeremiya anakhala mu nthawinso imene anakhala Zefaniya, Habakkuk, Danieli ndi Ezkieli. Utumiki wa uneneri unayamba mu chaka cha 626 B.C., ndipo unatha mu zaka za 586 B.C. Utumiki wake ukupitiriza utumiki wa Zefaniya, pokhala kuti Ezekieli anayamba utumiki wake ku Baibulo mu 593 B.C. Analinso mneneri amene anatumikira mofanana ndi mneneri wamkuru ameneyu ku Yerusalemu. Nthawi imene Yeremiya anamwalira sizimadziwika, ngakhale mbiri ndi zikhulupiliro za chiYuda zimanena kuti Yeremiya anaphedwa nthawi imene amakhala ku Aigupto (Ahebri 11:37).

Mutu ndi Cholinga: Mitu iwiri ndi iyi: (1) machenjezo a maweruzo a Mulungu potsatana ndi tchimo; (2) Uthenga wa chiyembekezo ndi kubwezeretsedwa ngati dziko litalapadi.

Anthu Ofunika: Yeremiya ndiye munthu wofunika mu bukhuli. Uthenga wake unali, kuziletsa ndi mazunzo.

Khristu mu Bukhu la Yeremiya: Zithunzi za Khristu zochuruka zikuonekera mu bukhu la Yeremiya. Akuonetsedwa ngati kasupe wa madzi a moyo (2:13 cf Yohane 4:14), mvunguti wa Gileadi (8:22), mbusa wabwino (23:4), Nthambi ya chilungamo (23:5), ndi mbuye wa chilungamo (23:6) akuwonedwanso monga amene adzabweretsa chipangano chatsopano (31:31-34).

Uneneri wina mu bukhu la Yeremiya uli ndi zovuta za tsogolo la Mesiya. Temberero la Yehoakini, Yekoniya (Yokoniya), limatanthauza kuti sipazapezeka wolandirana naye ufumu monga mwa thupi (22:28-30). Mateyu 1:1-17 akukamba za ndandanda wa mabadwidwe a Khristu kudzera mwa Solomu ndi Rehoboamu amene atate ake ali Yosefe (koma osati monga mwa thupi). Palibe mwana aliyense wa Yosefe amene adzathe kukhala pa mpando wa chifumu wa Davide pakuti adzakhala pansi pa temberero la Yehoakin. Luka 3:23-30 imafufuza mbiri ya kubadwa kwa Khristu kuchokera kwa Mariya, (makolo ake monga mwa thupi), kudzera mwa mwana wina wa Davide, Natani (Luka 3:31), ndipo pompo anapewa temberero. Nthambi ya choonadi idzalamulira pa mpando wa Davide.[38]

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Kuyitanidwa kwa Yeremiya, kuti Akhale Muneneri (1:1-19)**
   a. Maitanidwe (1:1-10)
   b. Masophenya oyamba Ayeremiya (1:11-19)

2. **Muneneri ku Yuda (2:1–45:5)**
   a. Chidzudzulo kwa Yuda (2:1–25:38)
      1) Ntchimo la Yuda (2:1–3:5)
      2) Kupanduka kwa Yuda (3:6–6:30)

3:6-10	4:19-31	6:1-21
3:11-25	5:1-13	6:22-30
4:1-18	5:14-31	

      3) Yuda apembedza Milungu ya Chilendo (7:1–10:25)

7:1-34	9:1-26
8:1-22	10:1-25

      4) Yuda aswa pangano la Mulungu (11:1–13:27)

11:1-17	12:1-6	13:1-11
11:18-23	12:7-17	13:12-27

      5) Chilala Ku Yuda (14:1–15:9)

14:1-12	14:13-22	15:1-9

6) Uneneri Ubweledzatso pa Yuda (15:10–16:13)
15:10-21 16:1-13
7) Machimo a Yuda (16:14–17:27)
16:14-21 17:1-18 17:19-27
8) Yuda ndi woumba mbiya (18:1-23)
9) Yuda ndi Tsupa woumba yosweka (19:1–20:18)
19:1-15 20:1-6 20:7-18
10) Mafumu a Yuda (21:1–23:8)
21:1-14 22:13-30
22:1-12 23:1-8
11) Aneneri onyenga Ayuda (23:9-40)
12) Yuda atengedwa ukapolo (24:1–25:38)
24:1-10 25:12-31
25:1-11 25:32-38

b. Yeremiya asusidwa (26:1–29:32)
1) Yankho p auneneri wa Yeremiya (26:1-24)
26:1-6 26:7-15 26:16-24
2) Langizo la Yeremiya kwa Yuda (27:1–29:32)
27:1-22 28:1-17 29:1-32

c. Chiyembekezo, yehova alonjeza kubweza kundende kwa anthu Asraeli (30:1–33:26)
30:1-17 31:27-40 33:1-13
30:18-24 32:1-15 33:14-26
31:1-26 32:16-44

d. Zochitika Yesusalemu asanapasuke (34:1–38:28)
34:1-22 36:20-26 38:1-16
35:1-11 36:27-32 38:17-28
35:12-19 37:1-10
36:1-19 37:11-21

e. Kugwa kwa Yerusalemu (39:1-18)
39:1-10 39:11-18

f. Zozhitika Yerusalemu atapasuka (40:1–45:5)
40:1-16 42:1-22 44:20-30
41:1-10 43:1-13 45:1-5
41:11-18 44:1-19

3. Uneneri kwa Mitundu (46:1–51:64)
a. Mauneneri pa Eguputo (46:1-28)
b. Mauneneri pa Afilisti (47:1-7)
c. Mauneneri pa Amoab (48:1-47)
d. Mauneneri pa Ammoni (49:1-6)
e. Mauneneri pa Edomu (49:7-22)
f. Mauneneri pa Damasiko (49:23-27)
g. Mauneneri pa Arabiya (49:28-33)
h. Mauneneri pa Elamu (49:34-39)
i. Mauneneri pa Baibulo (50:1–51:64)
50:1-20 50:41-46 51:27-44
50:21-32 51:1-10 51:45-58
50:33-40 51:11-26 51:59-64

4. Nkhani Zina (52:1-34)
a. Yerusalemu apasuka (52:1-23)
b. Chilango kwa Anthu (52:24-34)

Maliro
(Nyanja Yamisozi)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Wolemba wa bukhu la Maliro sanatchulidwe. Koma ndime ziwiri zimachitira umboni kuti Yeremiya ndiye mlembi wa bukhuli.

Mutu wa bukhuli ndi “Zachitika Bwanji?” Amene ndi mawu oyamba opezeka (1:1; 2:1; 4:1). Chifukwa nkhani zenizeni za mbukhuli, miyambo ya chiYuda linatchula bukhuli kuti “Maliro.”

Zaka: 586 Kapena 585 B.C. Pokhala bukhuli linalembedwa Yerusalemu atangoonongedwa kumene, mu 586; chaka chenicheni chimene linalembedwa ndi 586 B.C. Kafukufuku wa bukhuli akunena kuti bukhuli linalembedwa pakati pa 586 B.C. kapena 585 B.C.

Mutu ndi Cholinga: Mutu woyambirira wa bukhuli ndi kulira chifukwa cha ululu umene unagwerea ufumu wa kumwera kwa Yuda. Likufotokoza kuonongeka kwa Yerusalemu ndi Kachisi. Lonjezo la chiweruzo cha Mulungu pa Yuda chifukwa cha uchimo, lafika. Mutu wachwiri ndi chiweruzo chifukwa cha tchimo, pamenepo mneneri amadandaulira dziko kuti lidzindikire kuti kuli Mulingu, wachilungamo ndi choonadi mmachitidwe ake pa anthu ake, ndikuti amfunefune chifundo chake.

Chapaderanso chikuoneka mu Yeremiya ndi maliro zimaoneka pofananiza mabukhu awiriwa.[39]

Yeremiah (chenjezo) **Maso patso golo**	**Kugonjesedwa ndi Kutayidwa kwa Yerusalemu**	**Maliro** (kulira) **Kuyang'ana m'mbuyo**

Anthu Ofunika: Yeremiya

Khristu mu Bukhuli la Maliro: Maliro ali ndi zifanizo ziwiri zimene zimaonetsa mpulumutsi: (1) ngati munthu wazisoni, woonetsedwa, ndidziwidwa, ndi kudandaula, wonyozedwa, ndi wopwetekedwa ndi adani (1:12; 2:15-16; 3:14; 19:30); (2) Kulira kwa Yeremiya pa chionongeko cha Yerusalemu, ndi chithunzi cha Khristu amene analira, kulilira Yerusalemu (Mateyu 23:37-38).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Chionengoko ch Yerusalemu (1:1-22)**
   a. Kulira kwa meneneri (1:1-11)
   b. Kulira kwa mzinda wa Yerusalemu (1:12-22)

2. **Mkwiyoa wa Mulungu pa Anthu Ake (2:1-22)**
   a. Mkwiyo wa Mulungu (2:1-10)
   b. Kulira kwa Mlembi (2:11-22)

3. **Muneneri Achita Nkhawa (3:1-66)**
   a. Kulira kwake (3:1-18)
   b. Chiyembekezo chake (3:19-42)
   c. Kuvutika kwake (3:43-54)
   d. Pemphero lake (3:55-66)

4. **Tsoka pa Anthu a Yeresalemu (4:1-22)**
   a. Kulandidwa kwa Mzinda (4:1-12)
   b. Zifukwa zakulandidwa (4:13-20)
   c. Chiyembekezo cha tsogolo la bwino (4:21-22)

5. **Pemphero la Kubwezeletsedwa (5:1-22)**
   a. Kulapa 5:1-18)
   b. Kupempha /Pemphero (5:19-22)

Ezekieli

(Adzazindikira Kuti Ine Ndine YAHWEH)

Mlembi ndi Dzina: Wolemba bukhuli ndi Ezekieli, mwana wa Buzi amene analindira maitanidwe ake ngati mneneri akadali ku ukapolo wa ku Baibulo (1:1-3). Utumiki wake ngati mneneri, ukuonetsera kuyang'anitsitsa mwa unsembe ndi kukhuzika kwake pa Kachisi, ufumu, ndi ulemerero wa Mulungu. Zimene zikudziwika za Ezekieli, zikutengedwa mu bukhu lomweli la Ezekieli. Anali okwatira (24:15-18). Amakhala mu nyumba yakeyake (3:24; 8:1) ndi ena mwa akapolo anzake, anali kupezeka naye limodzi.

Monga mwa Yesaya ndi Yeremiya, bukhuli limatenga dzina lake kwa mlembi wake “Ezkieli” limene litanthauza “Mulungu amalimbikista” kapena “kulimbikisidwa ndi Mulungu.”

Zaka: 593–571 B.C. Bukhu la Ezkieli liri ndi masiku ambitri ndi cholinga choti mauneneri onse anaenedwe mu nthawi zoikika khumi ndi awiri. (12) a khumi ndi atatu (13), bukhuli limakamba za nthawi yomwe Ezkieli analandira mauthenga kwa Ambuye. Tsiku lina ndi lakufika kwa mtumiki amene analemba za kugwa kwa Yerusalemu (33:21). Kulandira maitanidwe ake mu July 593 B.C., Ezkieli anakhala wochitachita, kwa zaka 22. Mawu otsiriza anawalandira pafupifupi mu chaka cha 571 B.C.

Mutu ndi Cholinga: Ezekieli akunena moyang’anisitsa, “kutsutsidwa” (1–32) kwa Israeli ndi tchimo lake ndi chitonthozo (23:48) poyang’ana chomwe Mulungu adzachita mtsogolo.

Anthu Ofunika: Ezkieli mwana wa Buzi, wansembe woyitanidwa kukhala mneneri wa Israeli kumayambiliro ndi kumapeto kwa ukapolo.

Khristu mu Bukhuli: Khristu, Mesiya akuonetsedwa ngati mtengo umene uli pamwamba pa phiri (17:23-24), chithunzi chonga ngati cha nthambi ya Yesaya (11:1), Yeremiya (23:5; 33:15) ndi Zechariya (3:8; 6:12). Ezekieli amalankhulanso za mesiya monga mfumu yomwe ili ndi udindo ndi ufulu ndi ulamuliri (21:26-27) imenenso idzalamila ndi kuimilira ngati mbusa woona.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Kuyitanidwa kwa Ezekiel (1:1–3:27)**
   a. Ezekieli aona ulemelero wa Mulungu (1:1-28)
   1:1-21 1:22-28
   b. Ezekieli atumidwa ndi Mulungu. (2:1–3:27)
   2:1-10 3:1-15 3:16-27

2. **Chilango cha Yerusalemu ndi Yuda (4:1–24:27)**
   a. Zizindikiro zakubwera kwa Mesiya (4:1–5:17)
   4:1-8 4:9-17 5:1-17
   b. Mauthenga awiri akubwera kwa chiweluzo (6:1–7:27)
   6:1-14 7:1-19 7:20-27
   c. Mauneneri anayi kudzera mumasopsenya (8:1–11:25)
   8:1-18 10:1-22 11:14-25
   9:1-11 11:1-13
   d. Chiweruzo (12:1–24:27)
   12:1-28 17:1-10 21:18-32
   13:1-23 17:11-24 22:1-31
   14:1-11 18:1-32 23:1-21
   14:12-23 19:1-14 23:22-49
   15:1-8 20:1-32 24:1-14
   16:1-59 20:33-49 24:15-27
   16:60-63 21:1-17

3. **Mauneneri Odzudzula Amitundu (25:1–32:32)**
   a. Pa Ammoni (25:1-7)
   b. Pa Moabi (25:8-11)
   c. Pa Edomu (25:12-14)
   d. Pa Afilisiti (25:15-17)
   e. Pa Tulo (26:1–28:19)
   f. Pa Sidoni (28:20-26)
   g. Pa Eguputo (29:1–32:32)
   29:1-21 31:1-9 32:17-32
   30:1-19 31:10-18
   30:20-26 32:1-16

4. **Mauneneri Akubwezelesedwa kwa Aisraeli (33:1–48:35)**
   a. Israeli abwelera ku dziko la kwawo (33:1–39:29)
   33:1-20 36:1-21 37:24-28
   33:21-33 36:22-38 38:1-23
   34:1-10 37:1-10 39:1-24
   34:11-31 37:11-14 39:25-29
   35:1-15 37:15-23

b. Kubwezelesedwa kwa ufumu wa Israeli (40:1–48:35)

40:1-4	44:1-14	47:13-23
40:5-49	44:15-31	48:1-9
41:1-26	45:1-6	48:10-20
42:1-20	45:7-25	48:21-22
43:1-12	46:1-18	48:23-29
43:13-17	46:19-24	48:30-35
43:18-27	47:1-12	

Danieli

(Tsogolo Lotsiriza la Israyeli)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Mwa chitsimikizo cha Danieli mwini (12:4) mwa kagwiritsidwe ntchito ka mau "Ine" kuchokera ndime ya 7:2 kupita ku tsogolo. Danieli ndiye mlembi wa bukhuli. Adakali mnyamata, Danieli anatengedwa kupita kuukapolo ku Baibulo mu chaka cha 605 B.C. ndi Nebukadinezara. Kumeneko anakhala mzika mumabwalo a Nebukadinezara ndi Dariyo. Ngakhale sanatenge udindo wa uneneri, Khritu anamuzindikira iye kuti ndi Mneneri (Mateyu 24:15; Marko 13:14).

Bukhuli linatchulidwa dzina la mlembi wake, "Danieli" Limene limatanthauza "Mulungu ndi woweruza" kapena "Mulungu ndi woweruza wanga."

Zaka: 537 B.C. Bukhuli linalembedwa munthawi yaukapolo pamene Danieli ndi achichepere ena anatengedwa ukapolo mu chaka cha 605 B.C., Nebukadinezalali asanalande Yerusalemu.

Mutu ndi Cholinga: Mutu wa bukhuli ndi "mphamvu ya Mulungu wa mphamvu yonse" ndiye Mulungu mmodzi, woona, ndi woweruza ndi wophwasula mphamvu zooukira za dziko lonse, ndipo adzaombola mokhulupilika anthu ake, molingana ndi chikhulupiliro chawo mwa Iye. Bukhuli linalembedwa pofuna kulimbikitsa Ayuda a mundende kuzera mukuulula dongosolo la Mulungu wamphamvu pa Israeli mu nthawi yoyamba ndi kumapeto a kugwidwa ndi mphamvu za dziko lonse za amitundu.

Anthu Ofunika: Danieli amene anatengedwa wachichepere kukagwira ntchito m'mboma, komanso Shadreki, Misheki ndi Abedinego. Achinyamata ena atatu anasankhidwa ndi Danieli kuti alandire maphunziro apadera (maina awo oyamba achiyuda anali Hananiya, Michaelo ndi Azariya). Anthu ena ofunikira ndi Nebukadinezara mfumu ya Baibulo mu 605 B.C. Dariyo amene analindira ufumu Belisezara ngati mfumu Sira wolamulira ku Peresi ndi ngelo wotumizidwa ndi mikayeli ngelo wamkulu amene anatumikira Danieli mu gawo 10.

Khristu mu Bukhu la Danieli: Chimodzi mwa zithunzi za Khristu mu Danieli, ndi kubwera kwa Mesiya amene adzadulidwa, kufanizira ndi mtanda (9:25-26) komanso Khristu akuonetsedwa ngati mwala waululu umene udzaphwanya ufumu wa dziko lino (2:34-45), mwana wa munthu (7:13), wamasiku akale (7:22), masomphenya, monga alembedwa mubukhu la la Danieli 10:5-9 ndi ofanana ndi kuonekera kwa Khristu (Chivumbulutso 1:12-16).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Mbiri ya Danieli (1:1-21)**
   a. Ukapolo ku Baibulo (1:1-7)
   b. Kukhulupirika kwake (1:8-16)
   c. Mbiri yake yabwino (1:17-21)

2. **Uneneri (2:1–7:28)**
   a. Loto la Nebukadinezara (2:1-49)

2:1-18	2:36-38	2:44-45
2:19-30	2:39	2:46-49
2:31-35	2:40-43	

   b. Malawi amoto: Phunziro la chikhulupiliro (3:1-30)

3:1-7	3:8-18	3:19-30

   c. Loto la Nebukadinezala-mtengo waukuru (4:1-37)

4:1-3	4:19-27
4:4-18	4:28-37

   d. Madyerero a Nebukadinezara, Dzanja lolemba pa khoma (5:1-31)

5:1-12	5:13-29	5:30-31

e. Akalonga amunenezera Danieli kwa Dariyo (6:1-28)

6:1-15	6:16-28

f. Masomphenya a Danieli a Zamoyo zinayi (7:1-28)

7:1-8	7:13-14
7:9-12	7:15-28

3. Dongosolo la Mulungu pa Israeli (8:1–12:13)

a. Masomphenya a nkhosa yamphongo ndi Tonde (8:1-27)

8:1-8	8:15-19
8:9-14	8:20-27

b. Pemphero la Danieli (9:1-27)

9:1-19	9:20-23	9:24-27

c. Danieli aona masomphenya oopsa, Mngelo amulimbikitsa (10:1–12:13)

10:1-9	11:14-19	11:40-45
10:10-21	11:20-28	12:1-4
11:1-4	11:29-35	12:5-13
11:5-13	11:36-39	

Gawo 5
Mabukhu a Aneneri Aang'ono

Mawu akuti Aneneri a Ang'ono: Mutu wodziwika bwino wa mabukhu khumi ndi awiri awa ndiwo aneneri a ang'ono. Mutu uwu, unatumphuka mu 4th century A.D., aneneri awa ndi aang'ono chifukwa mauneneri awo ndi aafupi, kulekana ndi mauneneri a Yesaya, Yeremiya ndi Ezekieli, otchedwa "aneneri aakulu." Mu nthawi ya chipangano chakale ndi chatsopano; chipangano chakale chimatchedwa "chilamulo ndi anaeneri."

Chiyambi cha Ntchito ya Uneneri: Chiyambichi chikupezeka mu chifuniro cha Mulungu, pa Israyeli ngati dziko limene kudzera mwa ilo, maiko onse adzadalitsidwa, pamene Mulungu anapatsa Israyeli lamulo, amawalonjeza kuti akadzakhala omvera adzakhala anthu ***"Anga enieni"*** (Chuma cha mtengo wapatali cha Mulungu), ndi cholinga choti, adzakhala mu ufumu wa ansembe komanso pfuko loyera. Pakati pa mafuko onse, (Eksodo 19:5-6; Deut 4:6-8) cholinga ichi chidzalephereka ngati Israyeli atatsata zikhulupiliro za mapfuko ena. Pokonzekera kukalowa mu dziko la malonjezano, Mose asanamwalire, njira zosutsana ndi chilamulo ndi zaziwanda zogwiritsidwa ntchito ndi mafuko, kuumilira za tsogolo kapenanso chifuniro chenicheni cha Mulungu. Zopenduza, ula, kapena kubwebweta zinaletsedwa ndi Ambuye kudzera mwa Mose (Deuteronomo 18:15-22) amati:

> ***Ambuye Mulungu wanu adzakuutsirani pakati panu kuchokera mwa anthu anu., mnenere, muzamumvere iye. Iz ndi molingana ndi zones munapempha iye mu Horebu pa tsiku losonkhana ndkuti ndisazamvenso kuyankhula kwakukulu kwa ambuye Mulungu, ndisaonenso moto uwu waukulu, kuti ndingafe." Ndipo Mulungu anati kwa ine' wanena bwino, ndizadzutsa mneneri pakati pa amuna ngati iwe, ndipo ndidzaika mawu anga mkamwa mwake, ndipo adzalankhula zons zomwe ndidzamulamula, ndipo kudzakala kuti onse amene sazamvera mawu anga amene iye adzalankhula mu dzina langa, ine mwini ndidzafunsa za ichi. Koma mneneri amene adzalankhula mawu mongoyerekeza, amene sindinamutume mu dzina langa, kapena amene adzalankhula mudzina la milungu ina, mneneri ameneyo adzafa." Ndipo mudzanena mu mitima yanu, tidzadziwa bwanji mawu amene si Mulungu wanena? Pamene mneneri anenera mu dzina la Ambuye, ngati chinthucho sichikwaniritsidwa, chimenecho, Mulungu sanalankhule, sanachinenerre pa iye. Mneneriyo, wangolankhula pongoyerekeza, musamamuope wotereyo.***

Bvumbulutso ili, limapanga maziko a chiyambi cha Baibulo komanso chifukwa cha ntchito ya uneneri mu bukhu lopatulika. Komanso izi ziri chomwechi kuti dziko likakwaniritse chifuniro cha Mulungu monga mwa pangano la Abrahamu (Genesis 12:1-3). Adawapatsa malonjezano oikika ndi machenjezo. Izi zinalembedwa mu Deuteronomo 28-30 za madalitso ndi matemberero a mu magawo amenewa. Nthawi zina limatchedwa 'pangano la Palestina' pakuti pakumvera iwo adzakhala odala, pakusamvera, adzatembereredwa. Kodi aneneri mu chithunzi ichi apezekamo bwanji? Amatha kubwera ndikunena kuti ***"chifukwa anaswa pangano, matemberero ali paiwe, kapena atsala pang'ono kugwa pa iwe."*** kapena mwa njira ina, zachitika, "kapena ziri pafupi." Monga mmene Mulungu anachenjezera mu Deuteronomu 28-30, mauthenga a aneneri atchimo ndi chiweruzo amayenera awoneke poyera, ndi mmene bukhuli lafotokozera.

Aneneri sanangolankhula zochenjeza chabe, komanso uthenga wa chipulumutso ndi kudza kwa ulemelero wa Ambuye. Zolinga za Mulungu zikanakwaniritsidwa ndi ntchito za Mulungu mu miyoyo ya anthu ake. Nthawi zina mauthenga achipulumutso amatha kufotokoza za chochitika china chimene anaonapo masomphenya (Danieli 9:24-27) ndi mamasata 70. Nthawi zina amatha kulalikira malonjezano a Mulungu operekedwa kwa anthu ngati Abrahamu ndi Davide.

Zizindikiro za Aneneri a Ang'ono
Tikaphunzira aneneri onse, tipeza kuti ali ndi zoikika zowayenereza mkati: (1) chenjezo la chiweruzo chifukwa cha kuchimwa kwa maiko; (2) Kutanthauzira uchimo; (3) Tanthauzo la chiweruzo chiri nkudza; (4) Kuitanira kulapa; ndi (5) Lonjezo la kuomboledwa mtsogolo.

Mfungulo la kaganizidwe kabwino ka mbukhu la uneneri ndi kudziwa pamene maganizo enieni a neneri akuyambira kapena kuthera.[40] Aneneri amagwiritsa ntchito mawu otsogolera monga "ichi ndi chimene ambuye akunena" kenaka ndikutsiriza ndi mawu omwewo.

Mdandanda wa Aneneri Aang, Ono:

Aneneri Ang'ono-Ang'ono

1. Hoseya	4. Obadiya	7. Nahumu	10. Haggai
2. Yoweli	5. Yona	8. Habakkuku	11. Zekariya
3. AmosI	6. Mika	9. Zefaniya	12. Malaki

Kugawidwa Magulu Malingana ndi Ukapolo ndi Maufumu a Israeli ndi Yuda

Gulu	Bukhu	Nthawi (B.C.)
ASANATENGEDWE UKAPOLO: Aneneri a Israeli	Yona Amosi Hoseya	793–753 760 755–715
Aneneri a Yuda	Obadiyah Yoweri Mika Nahumu Zefaniya Habakkuku	840 835–796 700 633–612 630–625 600
UTATHA UKAPOLO: Aneneri a Otsalawo	Haggai Zekariya Malaki	520 520–518 450–400

Hoseya

(Kusunga Chikondi)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Hoseya mwana wa Beeri komanso mwamuna wa Gomeri (1:3) anali mzika ya kumpoto kwa Israeli. Pokhala chidwi chake, chinali kumpoto kwa Israeli ndipo anaitana mfumu yaku Samaria,'mfumu yathu' (7:5). Zonse za Hoseya timazipeza mu bukhuli.

Bukhuli linatchulidwa dzina la mlembi wake, Hoseya amene dzina lake ndi lofanana ndi mfumu yotsiriza ya dziko la Israeli, Hoseya. Pofuna kulekanitsa-Mbukhu lopatulika limatipatsa dzina la mneneri wang'ono Hoseya, chopatsa chidwa, maina a Hoseya; Yoswa ndi Yesu amatengedwa kuchokera ku dzina limodzi lachiyuda "HOSHEA," Amebe anatanthauza "chipulumutso" monga nthenga wa Mulungu, Hoseya akupereka chipulumutso kudziko ngati atabwerera kwa Mulungu.

Zaka: 755–715 B.C. Malingana ndi 1:1, Hoseya anatumikira masiku a mfumu Uzziah (767-739 B.C.), Yotamu (739-731 B.C.), Ahazi (731-715 B.C.), ndi Hezekiah (715-686 B.C.), mfumu ya Ai sraeli. Iye anatumikiranso mu masiku a Yeroboam II (782–752 B.C.), mfumu ya Israyeli.

Utumiki wa Hoseya unakula zaka zambiri, kuyambira pafupi mpaka mapeto a Uziya (767-739 B.C.) ndi Yeroboamu wachiwiri wa Israeli (739-753 B.C.) ndi kumangilira zaka zoyamba za ulamuliro wa Hezekiya Ulamuliro wotsirizawu unayamba chaka cha 715 B.C., itatha nthawi yakulamulira pamodzi ndi bamboo ake Ahazi. Pokhala Israeli linali dziko loyamba lachilendo kwa Hosea, zikudabwitsa kuti mafumu anai a ku Yudea, koma imodzi yak u Israeli kutchulidwa mu 1:1, chifukwa chochotsera mafumu 6, otsatira Yeroboamu. Mwina zitanthauza za ufumu wa Davide (3:5) pofananiza ndi kusakhazikika kwa ufumu wa kumpoto (7:3-7).[41]

Mwinanso, mafumu ena 6 a Israyeli omwe anatsatira Yeroboamu II anadumphidwa mwina anali osafunikira, komabe iwowo anachimwa aliyense payekhapayekha monga anachimwa Yerobuamu I, mwana wa Nebati. Pomwenso kunali mafumu a ku mpoto kwa i Israel yemwe anabweretsa kusintha ku ufumu wakumwera wa Yuda.

Mutu ndi Cholinga: Hosea analembedwa kuonetsera kuima mwangwiro pa chikondi cha mulungu pa Israeli ngakhale dzikoli linali losamvera. Kudzera mu ukwati wa Hoseya, bukhuli likutionetsera chikondi cha mulungu podalitsa anthu ake Hosea ndi mboni wamkulu wodzudzula ufumu wa kumpoto chifukwa dzikoli silinkamvera mulungu. Ndipo mneneriyu anaima kudzudzula pfukuli.

Anthu Ofunika: Hosea, Gomeri, Yehu Mfumu ya Israyeli

Khristu mu Bukhuli: Mbukhuli, Mesiya akuonetsera ngati Mwana wa Mulungu (11:1 cf. Mateyu 2:15) ngati mpulumutsi yekhayo wa anthu ake (13:4 cf. Yohane 14:6), ngati Iye amene adzatiukitsa kwakufa (13:14; 1 Akorinto 15:55), ngati iye amene amatikonda ndi chifundo chachikulu (11:4) ndi ngati iye amene adzachiritsa obwerera kwa iye (6:1).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Malonje (1:1)**

2. **Ukwati wa Hoseya: Kufanizira Zoipa za Israeli (1:2–3:5)**
   a. Banja la Hoseya, mu uneneri (1:2-11)
      1) Ukwati wa Hoseya: Kusakhulupilika kwa Israeli (1:2-3a)
      2) Ana a Hoseya: Chilango pa Israeli (1:3b-9)
      3) Tsogolo la Israeli: Kubwezeretsedwa (1:10-11)
   b. Kubwezeretsedwa kudzera mu chilango (2:1-23)
      1) Mulungu alanga Israeli (2:1-13)
      2) Mulungu abwezeretsanso Israeli (2:14-23)
   c. Kubwezeretsa mu nyumba ya Hoseya (3:1-5)
      1) Lamulo la Yehova (3:1)
      2) Kumvera kwa Hoseya (3:2-3)
      3) Kulongosola za mtsogolo (3:4-5)

3. **Uthenga wa Hoseya: Chiweruzo ndi Kubwezeretsa Israeli (4:1–14:9)**
   a. Mlandu pa Israeli (4:1-6:3)
      1) Tchimo la Israeli lionekera (4:1-19)
         4:1-3 4:7-10 4:15-19
         4:4-6 4:11-14
      2) Chiweruzo cha Israeli (5:1-15)
         5:1-7 5:8-15
      3) Anenera za kubwezeretsedwanso kwa Israeli (6:1-3)
   b. Mlandu wa Israel ukula (6:4–11:11)
      1) Tchimo ndi chilango cha Israeli (6:4–8:14)
         6:4-11 7:8-16 8:8-14
         7:1-7 8:1-7
      2) Tchimo ndi chilango cha Israeli (9:1–11:7)
         9:1-6 9:15-17 10:11-15
         9:7-9 10:1-2 11:1-4
         9:10-14 10:3-10 11:5-7
      3) Chifundo cha Yehova (11:8-11)
   c. Machenjezo pa Israeli (11:12–14:9)
      1) Chidzudzulo (11:12–13:16)
         13:1-3 13:9-11
         13:4-8 13:12-16
      2) Mulungu adandaulira Israeli alape, nalonjeza kuwakhululukira (14:1-9)
         14:1-3 14:4-7 14:8-9

Yoweli

(Kubwera kwa Tsiku la YAHWEH)

Mlembi ndi Dzina la Bukhuli: 1:1, akuonetsera kuti mlembi ndi Yoweri, mawu oti Yoweri amatanthauza kuti "YAHWEH ndi Mulungu." Dzina ili ndi lofunika poyang'ana uthenga wa Yoweri umene amatsindika kuti Mulungu ndi wamphamvu yonse ndi ulamuliro wake. Zambiri za yoweri sizidziwiko, koma bamboo ake anali Petueli (1:1).

Zaka: 835–796 B.C. Tsiku lnileni likupezeka mu bukhuli Anthu anakonza kuti 835–400 B.C. ndiye zaka zolemba Yoweri. Koma ife tikupereka 835–796 chifukwa cha zimene zinachitika kuTuro, Sidoni, Filisitiya, Aigupto, ndi Edomu, monga adani (3:4, 19). Awa anali adani oyambirira a ufumu wakumwera, asanalowe ku ukapolo ku Babulo, utatha undende wao, adani ao akadakhala Asuri, Babulo ndi Peresiya.

Mutu ndi Cholinga: Yoweri akugwiritsa ntchito njala ndi muliri wa dzombe umene unakantha, Yuda opanda chenjezo la kuonongedwa kwa Israyeli pa tsiku la YAHWEH. Munthawi yochepa, mumaola ochepa, chomera chirichonse chathedwa ndi dzombe koma ngati dziko lidzalapa, Mulungu azabwezeretsa ubale wake ndi iye.

Anthu Ofunika: Yoweri

Khristu Munkhaniyi: Khristu akuonesedwa ngatoi amene adzadzetsa mzimu, oyera (2:28 cf. Yohane 16:7-15; Machitidwe 1:8), woweruza (Mafuko 3:2, 12) amene ndi pothawira ndi chilimbikitso.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Tsiku Losaiwalika la Ambuye (1:1-20)**
   a. Dzombe (1:1-12)
      1:1-3 1:4-7 1:8-12
   b. Chilala (1:13-20)

2. **Uneneri (2:1–3:21)**
   a. Tsiku la Ambuye (2:1-27)
      1) Uneneri wa kulandidwa kwa Yuda (2:1-11)
      2) Zofunika kuti Yuda apulumuke (2:12-27)
         2:12-17 2:18-20 2:21-27
   b. Tsiku la Ambuye (2:28–3:21)
      1) Zochitika zotsiriza (2:28-32)
      2) Zochitika pa tsiku la Ambuye (3:1-21)
         3:1-8 3:9-17 3:18-21

Amosi

(Chiweruzo Pakusakhutitsidwa Kwawo)

Mlembi ndi Dzina la Bukhuli: Bukhuli linalembedwa ndi Amosi, Woweta ndi kusamalira chipatso cha mkuyu (1:1; 7:14). Anali wochokera ku Tekoa, pafupi ndi Betelehemu, moyandikana ndi Yerusalemu. Amosi anali wokhuzika ndi mawu a Mulungu.

Amosi ndi chihebri kutanthauza kuti "Goli" kapena "Onyamula Goli." Chimenechi ndi chomuyerekeza chifukwa cha Goli lomwe anali nalo lonyamula uthenga wotsusana ndi dyera, kupanda chilungamo, za dziko ndi kuziyenereza kwa ufumu wa kumpoto. Amosi yu, sanali Amozi, bambo a Yesaya (Yesaya 1:1).

Zaka: Pafupifupi **760 B.C.** Kolingana ndi 1:1, Amosi ndiye ananenera mu nthawi ya Uzziah, ndi Yeroboamu 2, ndi kunenera 790–739 B.C. Masiku a Uzziah, ku Yuda, komanso masiku a yeroboamu mfumu ya Israeli 793–753 B.C., Zaka ziwiri chivomerezo chisanachitike (1:1). Amosi anannenera mu 767–753 B.C. Tikuonanso kuti ananenera zaka ziwiri chivomerezo chisanachitike, koma tsiku lenileni silikudziwika.

Mutu ndi Cholinga: Uthenga wokhuza chiweruzo. Amosi anachenjeza kuti Mulungu azadza ngati wankhondo, kudzaweruza mafuko opandukira ulamuliro wake. Israeli mwapadera adzaonongeka chifukwa chophwanya pangano la Mulungu. Amosi anafuna kubweretsa mtundu wachuma umene unali pansi pa Yeroboamu kukulapa, kuti ikhale njira yokhayo yozembera chiweruzo chirinkuza. Mubukhuli tikuona kuipidwa kwa Mulungu pachoipa, popeza iye ndi woyera, ndikuti chilungamo chake chiyenera kuonekera pa Israeli, kutsutsana ndi tcimo lake, pakuti sangasiye Israeli asalangidwe pa tchimo lake. Mulungu adzasungabe gulu lina lolapadi (la Israyeli) limene limatchedwa lotsalira.

Tsiku lina gulu lochepa ili lidzabwezeretsedwa ku dziko lawo kuti akhale ndi Iye.

Anthu Ofunika: Amosi, Uziya, Yeroboamu, Mfumu ya Yuda, Mfumu ya Israyeli

Khristu mu Amosi: Amosi akuonetsera Khristu monga amene adzamangenso ufumu wa Davide (9:11) ndi amene adzabweretse anthu ake (9:11-15).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Malonje: Mlembi ndi Mutu wa Nkhani (1:1-2)**

2. **Zilango (1:3–2:16)**
   a. Zokhudza Damasiko (1:3-5)
   b. Zokhudza Afilisitia (1:6-8)
   c. Zokhudza Edomu (1:11-12)
   e. Zokhudza Ammon (1:13-15)
   f. Zokhudza Moabu (2:1-3)
   g. Zokhudza Yudah (2:4-5)
   h. Zokhudza Israyeli (2:6-16)

3. **Mauthenga a Amosi (3:1–6:14)**
   a. Chiweruza cha Israeli (3:1-15)
      3:1-8 3:9-10 3:11-15
   b. Kupsinjika (4:1-13)
      4:1-3 4:4-5 4:6-13
   c. Nyimbo ya maliro (5:1–6:14)
      1) Kuthyoka kwa Israeli (5:1-17)
         5:1-3 5:8-9 5:14-15
         5:4-7 5:10-13 5:16-17
      2) Chidzudzulo (5:18-27)
         5:18-20 5:21-24 5:25-27
      3) Aisraeli otsata zilakolako zao adza psinjika ndi mtundu wina wa anthu (6:1-14)
         6:1-3 6:8-11
         6:4-7 6:12-14

4. **Masomphenya a Amosi (7:1–9:10)**
   a. Masomphenya a Dzombe (7:1-3)
   b. Masomphenya a Moto (7:4-6)
   c. Masomphenya a chingwe (7:7-9)
   d. Chitsutso pa ansembe aku Beteli (7:10-17)
   e. Masomphenya a zipatso (8:1-14)
   f. Masomphenya a kulangidwa koopsa (9:1-10)

5. **Malonjezano Asano a Kubwezeretsedwa kwa Israeli (9:11-15)**

Obadiya

(Chilungamo, Ndakatulo)

Dzina ndi Mlembi wa Bukhu: Malinga ndi bukhuli (1:1) Obadiya ndiye mlembi wake Obadiya atanthauza "Mtumiki, kapena Opembeza YAHWEH."

Anthu angapo muchipangano chakale anatchulidwa dzina la Obadiya, awa ndi monga: Kazembe wankhondo wa mfumu Davide (1 Mbiri 12:9); Kapolo wa Ahabu amene anasunga mobisa, aneneri a Mulungu (1 Mafumu 18:3) mlevi, masiku a Yosiya (2 Mbiri 34:12) ndi mtsogoleri amene anabwerera kuukapolo ndi Ezara (Ezara 8:9). Palibe chomwe chikudziwika cha Obadiya chokhuza dera lomwe amachokera, kapenanso banjalake, ndipo chifukwa chakuti bamboo ake sanafotokozedwe, koma tikhoza kuganiza kuti sanali ochokera ku banja lachifumu kapena unsembe.

Zaka: 840 B.C. Bukhu lalifupi kwambiri mu bukhu lopatulika lokhala ndi ndime 21 basi. Ndilosiyana ndi mabukhu ena a aneneri aang'ono chakachi chikudziwika chifukwa chauneneri wotsutsana ndi Edomu ndi Arabiya ndi Afilisitiya, umene umaoneka ngati wa nthawi ya Yehoramu 848–841 B.C. (2 Mbiri 21:16-27).

Mutu ndi Cholinga: Mutu wa Obadiya ndi choonadi chakuti "kuzikunza kumabwerera koyamba munthu asanagwe." Obadia akutsindika kuti Edomu waima woweruzidwa chifukwa cha kuzikuza kwake, kunyadirira choipa chochitika pa Yerusalemu.

Anthu Ofunika: Obadiya

Khristu mu Obadiya: Khristu akuoneka mu bukhuli ngati woweruza maiko onse (15-16), Mpulumutsi wa Israeli (17-20); Mwini waufumu (21).[42]

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Uneneri wa Chilango cha Edomu (1:1-9)**
   a. Zeni zeni za chilango (1:1-4)
   b. Chilango chonse (1:5-9)

2. **Kulangidwa kwa Edomu (1:10-14)**
   a. Kusowa chikondi/ chiwawa (1:10)
   b. Matama/ kuzikonda (1:11-12)
   c. Ukali ndi Mtopola (1:13-14)

3. **Tsiku la Yehova (1:15)**

4. **Zotsatira za Chigamulo (1:16-18)**

5. **Kuwomboledwa kwa Israeli (1:19-21)**

Yona
(Kuzemba Mulungu)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Mlembi wa Bukhu ndi Yona, mwana wa Amittai, mneneri wochokera ku Galileya, kumpoto wa Israeli. Izi zikupezeka mu bukhuli (1:1), munthu amene akuoneka mu mbiri ya bukhuli imene idzatchula zenizeni, (2 Mafumu 14:25) kuphatikizanso umboni wa Ambuye Yesu muchipangano chatsopano (Mateyu 12:40) dzina lake limatanthauza "nkhunda."

Zaka: 793–753 B.C. Mu bukhula 2 Mafumu 14:27, Yona akulumkizidwa ndi kukhudzana kwa Yeroboamu 2 wa ku Israyeli (791–753 B.C.). Yona anatumikira itatha nthawi ya Elisa, komanso isanafike nthawi ya Hoseya ndi Amosi.

Mutu ndi Cholinga: Yona akuonetsa kuti khalidwe lopanda chikondi pakati pa mitundu yosiyanasiyana, lingathe kutchinga anthu kuti alephere kutsatira chifuniro cha Mulungu, ndi Mulungu wa Yuda (1:1) ndi okhudzika ndi dziko lonse, pakuti chipulumutso chapatsidwa kwa onse, natembenukira kwa iye, ndipo ndiopambana zolengedwa ndi zochitika zonse za anthu.

Anthu Ofunika: Yona

Khristu mu Bukhuli: Kudzera mwa Yona, Khristu akuonetseredwa mukuuka kwake (Mateyu 12:40) monga mneneri wamafuko (ngakhale iye sanali onyozera ngati Yona). Ndipo ngati mpulumutsi ku maiko, mumoyo wa Yona Khristu akuonedwa ngati mpulumutsi ndi Ambuye (2:9).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Kuzemba Mulungu (1:1-17)**
   a. Chifukwa chomwe ana zembera Mulungu (1:1-2)
   b. Njira yomwe anadera Yona (1:3)
   c. Chotsatira cha kuthawa Mulungu (1:4-17)

2. **Pemphero la Yona (2:1-10)**
   a. Kapempheredwe (2:1-9)
   b. Yankho la pemphero (2:10)

3. **Yona Alalikira Uthenga (3:1-10)**
   a. Mulungu alamula Yona (3:1-3)
   b. Uthenga womwe Yona analalika (3:4)
   c. Zotsatira za ulaliki wa Yona (3:5-10)

4. **Phunziro la Yona (4:1-11)**
   a. Yona amudandaulira Mulungu (4:1-3)
   b. Chiphunzitso cha Mulungu kwa Yona (4:4-11)

Mika
(Ndani Angafane ndi Mulungu?)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Bukhuli linatenga dzina kuchokera kwa mlembi wake Mika mneneriyo. Zochepa zokha zimadziwika za mlembiyu (Yeremiya 26:28). Dzina la Mika ndi chidule cha dzina Mikaya limene limatanthauza "ndani wofanana ndi YAHWEH?" Mika akufunsa choonadi ichi mu 7:18 pamene akuti "Ndi ndani Mulungu onga inu?" Oa Mika 3:12, akuikira kumbuyo uthenga wa Yeremiya wa chiweruzo ku dziko (Yeremiya 26:18).

Mika adali wochokera ku moresiti (Mika 1:1 cf. 1:14), Yudeya pafupi miringo 25, kumwera kwa Yerusalemu pafupi ndi afilisiti wa Gati. Moresiti ndidera lokhala mphepete mwaphiri la lashishi, malo amlonda a dziko.

Zaka: 700 B.C. Mu vesi 1:1 tikuona kuti ananenera mu nthawi ya Yotamu (750–732 B.C.), Ahazi (736–716 B.C.), ndi Hezekiya (716–681 B.C.). Mika akuyankhula koyamba kwa Yuda, koma chifukwa akulankhulanso kwa Israeli ndi kulosera kugwa kwa Samariya (1:6), mbali yautumiki wake inaonekera pa ukapolo wa Assuril mu 722 B.C., mu nthawi ndi zaka pafupifupi 700 B.C.

Mutu ndi Cholinga: Mika akuonetsa momwe anthu analepherera kukhala mkati mwa pangano ndi zofunika za pangano limene Mulungu adapanga ndi Aisrayeli m'mene mukadakhala dalitso la kumvera kwawo (Deut 28:1-14). Temberero chifukwa cha kusamva ndi kutulutsidwa ku dziko lalonjezo (Deut 28:15-68). Mkatimo, Mika adalongosola za kusowa chilungamo kwa Yuda ndi kukhazikitsa choonadi cha YAHWEH, kuonetsera kupereka mwambo kwa iwo. Akubweretsanso zigamulo, kutsutsana ndi Yuda pamachimo opondereza, ziphuphu, pakati pa oweruza, aneneri, ndi ansembe, ndi mabodza, kusirira, kuzikudza ndi chiwawa. Ndi zoona kuti mwambo umenewu pa fukoli unaonetsera chikondi cha Mulungu pa iwo ndi kuti akadatha kuwabwezeretsa.

Mutu wachiweruzo ndi weniweni mu mauthenga atatu onse, koma anatsindikanso choonadi cha kubwezeretsedwa mopitilira. Mika amalankhula mopitiriza mfundo mu mauthenga ake onse (Mika 2:12; 4:7; 5:7-8; 7:18). Anasindikiza kuti tsogolo Yahweh azabwezeretsa Israyeli ku malonjezo pa kubwera kwa Mesiya.

Gawo lotseka bukhu la Mika likufotokoza nkhani pa bwalo la milandu. Mulungu ali ndi nkhani yaikulu ndi anthu ake ndipo akuitana mapiri ndi zitunda pamodzi kuti zipange gulu la oweruza pamene akubweretsa mulandu wake. Anthu osinthanitsa kupembeza koona, ndi mafano achabe, naleka njira zachilungamo cha Mulungu, ndi cholinga chakuti aphimbe chinyengo chawo. Pakhoza kukhala chigamulo chimodzi chokha chomwe ndi mawu akuti "ochimwa."

Bukhuli limatsekedwa pakupereka chiyembekezo. Mulungu wopereka maweruzoyo, amaonetseranso chfundo, ***"ndani afana nanu Ambuye kukhululuka ndi kusalabada zolakwa? Sasunga mkwiyo wake kwamuyaya chifukwa amakondwerere mu zifundo"*** (7:18). Choncho ndizapenyerera pa ambuye, ***"kuyembekezera Mulungu wa chipulumutso changa, Mulungu wanga adzndimva"*** (7:7).[43]

Anthu Ofunika: Mika, Yoramu, Ahazi, Hezekiya

Khristu mu Bukhuli: Mika akuonetsera Khristu monga Mulungu wa Yakobo (4:2), oweruza mafuko (4:3), ndi olamula amene azabadwira mu mzinda wa Beteli (5:2 cf. Mateyu 2:1-6). Ansembe ndi Asaduki anagwirita ntchito mawu a Mika pa (5:2) poyankha funso la herodi pazakubadwa kwa Mesiya.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Malonje (1:1)**

2. **Uthenga Woyamba: Mau Akuchenjeza Israeli ndi Yuda Chifukwa cha Machismo Ao (1:1–2:13)**
   a. Kulosera za chiweruza (1:2-7)
   b. Kulilira anthu (1:8-16)
      1) Kulira kwa Mika (1:8-9)
      2) Mika apempha anthu onse kuti alire kwa Mulungu (1:10-16)
   c. Tchimo la Yuda (2:1-11)
      1) Tchimo la anthu (2:1-5)
      2) Tchimo la aneneri onyenga (2:6-11)
   d. Kulosera kukumana kwa anthu mtsogolo (2:12-13)

3. **Uthenga Wachiwiri: Chiwombolo (3:1–5:15)**
   a. Chiweruzo pa atsogoleri a Dziko (3:1-12)
      1) Chiweruzo pa olamulira (3:1-4)
      2) Chiweruzo pa aneneri onyenga (3:5-8)
      3) Chiweruzo pa atsogoleri opulukira (3:9-12)
   b. Madalitso (4:1–5:15)
      1) Maonekedwe a ufumu 4:1-8)
      2) Nkhani zina (4:9–5:1)
      3) Wolamulira (5:2-15)

4. **Uthenga Wachitatu: Mulungu Atsutsana ndi Anthu pa Zoipa Zawo (6:1–7:20)**
   a. Chiweruzo (6:1-5)
   b. Yankho la Mika pa pfuko (6:6-8)

c. Chilango cha Mulungu (6:9-16)
   1) Uchimo (6:9-12)
   2) Chilango (6:13-16)
d. Mika apempha chifundo cha Mulungu (7:1-17)
   1) Mika alilira tchimo la pfuko (7:1-6)
   2) Chikhulupiliro cha Mika pa Mulungu (7:7-13)
   3) Pemphero la Mika (7:14)
   4) Lonjezo la Mulungu (7:15-17)
e. Mika atsindika za Mulungu (7:18-20)

Nahumu

(Chiweruzo cha Ninevi)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Nahumu 1:1, akunena kuti bukhuli ndi la masomphenya a Nahumu mu Elikosite ndiliu lofotokoza za neneve. Nahumu amatanthauza "chitonthozo" koma uthenga wake sunali wokhuza kutonthoza kwa Asuri oipawo amene anatenga malo mu Ninevi. Zikanatheka kuti abweretse kumapeto kwake, chitonthozo cha ku a Yuda, ndizotheka kuti akanakhalanso mneneri wa aYuda. Poona 1:15 ngakhale malo enieni a Elokosi, ndi osadziwika; ophunzira ambiri amati mzinda umenewu uli kumwera kwa Yuda.

Monga mwa aneneri onse aang'ono, bukhuli linatenga dzina kwa mneneri amene anayankhula uneneriwu.

Zaka: 663–612 B.C. Nahumu amalankhula za kugwa kwa Tibesi ku Aigupto monga mwa 3:8-10. Tibesi anagwa mu 663 B.C. Mu magawo onse atatu, Nahumu analankhula zakugwako kumapeto kwanthawi chifukwa akufotokoza kugwa kwa Ninevi ngati kwadzidzidzi (2:1; 3:14, 19). Ichi chingathe kuika utumiki wake munthawi ya ulamuliro wa mfumu Yosiya ndi kumupanga kukhala wotumikira limodzi ndi Zefaniya ndi Yeremiya.

Mutu ndi Cholinga: Kugwa kwa Ninevi, monga kubwezera kwa Mulungu kutsutsana ndi Asuri oipa wa ku Ninevi. Chimene Yona ankafuna kuona, monga chiweruzo cha Mulungu pa Asuri, chinanenedweratu ndi Nahumu, pafupifupi zaka 150 kutsogolo.

Kukambirana kwa a ninevi poyankha kulalikira kwa Yona zinachitika posachedwa, chifukwa posakhalitsa, anakhala popanda chisoni, kubwerera ku zoipa zao zapoyamba. Sagon 2 wa ku Asuri, anaononga Samariya, ndikutenga mfumu ya Israeli ndi ktenga kuukapolo, kumwaza mafuko khumi ndi awiri mu 722 B.C. Kenako Senakerubi wa ku Asuri anali pafupi kugwira yerusalemu nthawi wa Hezekiya mu 701 B.C. Posatengera za mphamvu ndi kudziwika kwake, Ninevi waweruzidwa momveka bwino mona watsekeredwa ndi Mulungu kudzera kwa Nahumu. Ngakhale bukhuli limayang'anisitsa za kugwa kwa Asuri ndi chiweruzo, linalembedwa kubweretsa chitonthozo ku Yuda.

Anthu Ofunika: Nahumu

Khristu mu Nahumi: Ngakhale palibe ulosi weniweni wa Khristu mu Nahumu, koma mu kusunga ulosi, pali chithunzi choti Khristu ndi Mulungu wansanje wakulanga anthu osamvera (1:2-13).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Malonje (1:1)**

2. **Mauneneri ndi Zoonadi za Chiweruzo cha Mulungu pa Nineveh (1:2-15)**
   a. Chilango ku Nineveh (1:2-8)
   b. Kugalukira kwa Ninevi pa YAHWEH kuzatha (1:9-11)
   c. Chizunzo cha Yuda chidzatha chifukwa cha chiweruzo cha Nineveh (1:12-15)

3. **Kulangidwa kwa Ninevi (2:1-13)**
   a. Nkhanza ilongosoledwa (2:1-6)
   b. Kugonjetsedwa (2:7-13)

4. **Kupasuka kwa Nineveh (3:1-19)**
   a. Chiwawa ndi chunyengo chake (3:1-7)
   b. Zochita zake (3:8-11)
   c. Kuziteteza kwake, nkopanda ntchito (3:12-19)

Habakuku
(Yankho pa Chisokonezo)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Mlembi wa bukhuli ndi Habakuku monga momwe afotokozera mu 1:1 ndi 3:1. Mlembiyu ndi mneneri ndipo akumaliza ndi mawu a pembezero oti, ***"kwa Woyimba wamkulu, woyimbira zida za zingwe"*** akulongosola mwa unsembe.

Bukhuli latenga dzina lake kuchokera kwa mlembi wake Habakuku dzina la chihebri lomwe limatanthauza kukakamira. Mneneriyo akukakamira pa YAHWEH monga Mulungu wa chipulumutso ndi mphamvu zake.

Zaka: 600 B.C. Chifukwa bukhuli limanena za kubwera kwa Ababulo kuzaononga pfuko, izi zikusonyeza kuti Habakuku analemba bukhuli mu nthawi ya ulamuliro wa Yehoakim mfumu ya Yuda. Zikuonekanso kuti pa nthawiyi inali nthawi yomwe Babulo anali asanatenge Yuda (1:6; 2:1), zomwe zikusonyeza ulosi wa babulo mu 605 B.C.

Mutu ndi Cholinga: Mutu wa bukhuli unagona pa kusokonezeka mutu pa nkhani za Babulo. Panali nkhani monga izi: (1) Chifukwa chiyani mulungu analola kuti Yuda apitilire kulakwa komanso asalangidwe (1:2-4)? (2) Kodi mulungu woyera (1:13) angagwiritse bwanji ntchito Babulo polanga dziko lina (1:12–2:1)? Habakkuku samamvesetsa kuti zikuyenda bwanji komanso iyeyu akupereka mfundo zoteteza ubwino wa Mulungu ndi mphamvu zake ngakhale anthu atachimwa.

Anthu Ofunika: Habakuku

Khristu mu Habakuku: Mu maulosiwa, Khristu akusonyeza mpulumutsi. Mawu oti chipulumutso, omwe akupezeka mu 3:13 ndi 18, ndi mawu a muzu omwe akuimilira Khristu mu (Mateyu 1:21). Akuonekanso monga Woyera (1:12 cf. 1 Yohane 1:9), Yemwe akulungamitsa anthu mu njira yoyenera mwa chikhulupiliro (2:4) ndi yemwe tsiku lina azazadzitsa dziko lonse ndi ***"Chidziwitso cha ulemelero wa Ambuye monga madzi ozadza mu nyanja"*** (2:14).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Malonje (1:1)**

2. **Katundu Adamuona Habakuku: Chikhulupiliro Chimayesedwa ndi Kuphunzitsidwa (1:2–2:20)**
   a. Bvuto loyamba: Nchifukwa chiyani Mulungu akulola zoipa kuchitikabe mu Yuda? (1:2-4)
   b. Yankho loyamba la Mulungu (1:5-11)
   c. Funso lachiwiri: Chifukwa chiyani Mulungu adzagwiritsa ntchito ochimwa kulanga Yuda? (1:12–2:1)
   d. Yankho lachiwiri la Mulungu (2:2-20)

3. **Matamando a Habakuku: Chikhulupiliro ndi Chimwemwe (3:1-19)**
   a. Matamando pa munthu wa Mulungu (3:1-3)
   b. Matamando pa mphamvu ya Mulungu (3:4-7)
   c. Matamando pa cholinga cha Mulungu (3:8-16)
   d. Matamando pa Chikhulupiliro mwa Mulungu (3:17-19)

Zefaniya
(Madalitso Kudzera mu Chigamulo)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Monga alemba mu 1:1, mlembi ndi Zefaniya, mwana wa Kusi, mwana wa Gedaliya, mwana wa Amariya, mwana wa Hezekiya. Polongosola za mbadwo, zikuonetseratu kuti bukhuli ndi losiyana ndi anzake. Kawirikawiri, bambo wake wa m'neneri ndi yemwe amatchulidwa osati ndi agogo omwe (Yesaya 1:1; Yeremiya 1:1; Ezekiel 1:3; Hoseya 1:1; Yoweli 1:1) pomwe mlembi akulongosola mibadwo kuti. Mlembiyu agogo ake angapo analinso aneneri, komanso akulongosola za mfumu Hezekiya wabwinoyo.

Bukhuli linatenga dzina la mlembi wake lomwe likutanthauza "zobisika za YAHWEH'' (2:3).

Zaka: 630–625 B.C. Malinga ndi malonj (1:10), Zephaniy analosera pa ullamuliro wa Yosiya mu (640–609 B.C.). Uneneri wake unalingana ndi kugwa kwa Ninevi mu 612 B.C.ndi ulamuliro wa Yosiya mu 622–621 B.C. Izi zikusonyeza kuti bukhuli linalembedwa nthawi yomwe anthu ankapembeza mafano kwambiri mu Yuda (1:4-6) zomwe zinathetsedwa ndi Yosiya mu zaka za 630 ndi 625 B.C.

Mutu ndi Cholinga: Mneneriyu akulankhula kwa anthu a Yuda yemwe khalidwe lake ndi uzimu wake unali woipa mu ulamuliro wa Manasseh ndI Amon (3:1-7). Pofuna kupitilira kuchenjeza za matemberero a mu Deuteronomu 28, mutu weniweni ndi wa chilango komanso kudzanso kwa Ambuye. Malinga ndi kuyera kwa YAHWEH, iye adzaombola ndi kuonetsera kuyera kwake podzudzula tchimo la mafuko ndi kupereka lonjezo kwa omukhulupilira, choncho bukhu la Zefaniya likugawidwa mu zigawo zitatu. Chilango pa tchimo, kuitanira anthu ku kulapa, ndi lonjezo la mdalitso wa chiombolo.

Anthu Ofunika: Zefaniya, Yosiya

Khristu mu Zefaniya: Ngakhale Khristu sanatchulidwe mu bukhuli, mesiya akuimiliridwa ndi mawu oti "Woyerayo'' mu mafuko a Israyeli (3:5) yemwe ali mfumu yawo (3:15).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Malonje (1:1)**

2. **Chiweruzo pa Tsiku la YAHWEH (1:2–3:8)**
   a. Chiweruzo pa dziko lapansi (1:2-3)
   b. Chiweruzo pa Yuda (1:4–2:3)
      1) Zoyambitsa chiweruzo (1:4-13)
      2) Kalongosoledwe ka chigamulo (1:14-18)
      3) Mawu akuchenjeza -lapani, bwererani kwa Mulungu (2:1-3)
   c. Mawu akuchenjeza maiko ena (2:4-15)
      1) Dziko la Afilisiti (2:4-7)
      2) Dziko la Moabu ndi Amoni (2:8-11)
      3) Dziko la Akusi (Ethiopia) (2:12)
      4) Dziko la Assuri (Ninevi) (2:13-15)
   d. Mawu akudzudzula Yerusalemu (3:1-7)
      1) Mneneri onyenga (3:1-5)
      2) Chiweruzo cha Yehova (3:6-7)
   e. Mkwiyo wa Yehova pa Amitundu (3:8)

3. **Kubwezeretsedwa pa Tsiku la YAHWEH (3:9-20)**
   a. Kubwezeretsedwa kwa mayiko (3:9-10)
   b. Kubwezeretsedwa kwa Israel (3:11-20)

Hagai
(Chilimbikitso)

Malonje: Ndi Hagai, tikufika pa mmodzi w aneneri atatu omwe analemba atabwerako kotengedwa ku ukapolo wa Babulo ndipo mabukhuwo ndi awa: Haggai, Zekariya, ndi Malaki, zonse zimalongosola za Ayuda omwe anabwerera kuchokera ku ukapolo ndikupita ku Israeli. Cholinga cha ulosiwu chinali cholimbikitsa anthu mu uzimu ndi kuthupi, anthu omwe anabwerera kudziko lawo kuchoka ku ukapolo, ndipo amafuna kumanganso Kachisi ndi pfuko lawo.

Haggai ndi Zekariya analongosola kwambiri zauzimu ndi kumanganso kachisi ndipo malaki analongosola za makhalidwe a anthu pofuna kumanganso pfuko lawo

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Dzina loti Hagai likuimilira "Chikondwerero'' kutanthauza kuti anabadwa mu nyengo ya maphwando, ngakhale izi sizinalembedwemo. Hagai watchulidwa mu bukhuli ka 9 ndipo watchulidwa mu bukhu la Ezara 5:1-2 ndi 6:14. Za mneneri Hagai (1:1), zakambidwa koma za mbadwo sizinalembedwemo. Iye anatsatira Zekariya Mneneri ndi Zerubabelo Chiwanga.

Ndipo bukhuli latenga dzina lake kuchokera pa Mlembiyo yemwenso ndi mneneri.

Zaka: 520 B.C. Mu ulamuliro wa Cyrus, Mfumu ya a Perezi pafupifupi ayuda 50,000 analoledwa kubwerera kwawo ndipo mkati mwa anthuwa munali Zerubbabel (Ezara 1:2-4 cf. Yesaya 44:28), Yoswa wansembe wamkuluyo ndi aneneri monga Haggai ndi Zekariya. Ayuda analoledwa kupita kwawo kukamanga kachisi mu chaka cha 538 B.C.

Nsembe za Alevi zinakhazikitsidwanso pa nsanja ya nsembe yopsereza yomwe inamangidwayo (Ezara 3:1-6), ndipo mu chaka chachiwiri cha kubwereranso ndi kumanganso kwa Kachisi (Ezara 3:8-13; 5:16). Komabe,

kuchita nkhanza kwa Peresi zinabweretsa kumangidwanso kwa Kachisi. Mu zaka zina zokwana khumi ndi zisanu ndi mphambu imodzi (16)–kufikila mu ulamuliro wa Peresi, Daliyo Hystaspes (521-486 B.C.)–mamangidwe a Kachisi anapitilirabe. Mu chaka chachiwiri cha Daliyo (520 B.C), Mulungu anautsa m'neneri Hagai kuti alimbikitse mtundu wa Chiyuda kupitiliza kumanganso kwa Kachisi (Ezara 5:1-2; Hagai 1:1).

Monga kunanenedwa ndi mneneri Hagai 1:1, uthenga wake unaperekedwa tsiku loyamaba la mwezi wa (Elul) (August –September) mu chaka chachiwiri cha ulamuliro wa Dariyo. Ichi chinali chaka cha 520 B.C.

Mutu ndi Cholinga: Buku la Hagai ndi buku lachiwiri lalifupi kuchokera ku buku la Obadiya. Buku ili linalembedwa mwachindunji ndi mophweka kulimvetsa. Mu bukhuli muli malipoti a mauneneri omwe amaoneka ngati osafunikira.

Ngakhale Haggai liri bukhu lachiwiri lalifupi mu chipangano chakale, sitiyenera kunyozetsa mphamvu za mauthenga anayi a Hagai pa ntchito yakumanganso kachisi. Aneneri owerengeka okha ndi omwe athandizira kuti uthenga wa mu bukhu ili ukhale wamphamvu. Zina mwa zokambidwa mu Hagai zidali zamphamvu zochokera kwa Mulungu ndipo nthawi zokwana 25, iye wakambapo uthenga wa ulamuliro woyera wa Mulungu. Ndipo iye wapitiliranso kupereka malonje motere: ***"Izi ndi zomwe ambuye Wanena"*** ndipo amatsiriza ndi mawu oti: ***"Walengeza ambuye Wamakamu."***

Hagai analemba polimbikitsa otsalawo a Israeli pa kumangansi kachisi ku Yerusalemu. Mu njira yotero iye anaphunzitsa kuti (1) Mulungu amadalitsa anthu ake iwo akamuika Iye patsogolo, (2) Sitiyenera kutopa mukuchita ntchito zabwino ndi (3) Malonjezo a Mulungu a mawa asanduka maziko a chitsimikizo cha lero.

Anthu Ofunika: Haggai, Dariyo, Zerubabelo, Yoshua Wansembe wamkulu

Khristu mu Bukhu la Haggai: Mu bukhu ili, Mesiya akuonetseredwa monga Wobwezeretsanso Kachisi waulemelero (2:7-9) komanso Yemwe adzapambane maufumu onse a dziko lapansi (2:22).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Uthenga Woyamba: Kuitanidwa Kukamanga Kachisi (1:1-15)**
   a. Malonje (1:1)
   b. Chidzudzulo choyamba (1:2-6)
   c. Kupeza yankho (1:7-8)
   d. Chidzudzulo cha chiwiri (1:9-11)
   e. Kuvomereza uthenga wa mneneri (1:12-15)

2. **Uthenga Wachiwiri: Chilimbikitso pa Malonjezano a Mulungu (2:1-9)**
   a. Malonje (2:1-2)
   b. Malonjezo a ulemelero wa Mtsogolo (2:3-9)

3 **Uthenga Wachitatu: Kuyeretsa Moyo (2:10-19)**
   a. Malonje (2:10)
   b. Bvuto: Kusamvera kwa otsalawo (2:11-14)
   c. Mthetsa Bvuto: Kumvera kwa otsalawo (2:15-19)

4. **Uthenga Wachinayi: Apempha Chikhulupiliro pa Tsogolo Lawo (2:20-23)**
   a. Malonje/ chiyambi (2:20-21a)
   b. Lonjezo la kugonjetsa ufumu wa amitundu (2:21b-22)
   c. Lonjezo la kubwezeretsedwa kwa ufumu wa Davide (2:23)

Zekariya
(Nsanje ya YAHWEH)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Mlembi anali mneneri Zekariya, mwana wa Bekariya, mwana wa Iddo, (Zekariya 1:1). Anali mzake wa Haggai (Ezara 6:14).

Mawu oti Zekariya amatanthauza kuti "YAHWEH Amakumbuka'' kapena kuti "YAHWEH watikumbuka.'' Ndipo mutu uwu wakambidwa mu bukhu lonseli.

Zaka: 520-518 B.C. Vesi loyamba likukamba za Zekariya kuti anali mwana wa Berikaya, mdzukulu wa Iddo, yemwe anali wansembe wotchulidwa mu Nehemiya 12:4, mzake wa Zerubabelo. Mu Zekariya 2:4, mneneri

akutchula monga mnyamata. Iye anali mnyamata pa nthawi ya kumanganso mu 520 B.C. (7:1-14) mu 518 B.C. (9–14) akulongosolanso nkhani ina, ndipo mu 880 B.C. akukambanso zina (9:13).

Palibe nkhani zambiri za Zekariya mu mabukhu ena koma mu Mateyu 23:35 pomwe akunena kuti Iye anaphedwa ndi anthu pa nkhani za mu kachisi. Ndipo Zekariya winanso, mwana wa wansembe wotchedwa Yoida, anaphedwa mu nthawi yomweyo (2 Mbiri 24:20-21).[44]

Mutu ndi Cholinga: Bukhu la Zekariya linalembedwa pofuna kulimbikitsa otsalawo omwe anabwerera ku ukapolo, kuti amangenso kachisi wa Yehova. Mneneriyo anawaonesetseranso kuti Mulungu anali kugwira ntchito yake pa iwo yobwezeretsa Israeli kuti akonzekeresedwe ku kubwerera kwa Mesiya. Chiphunzitso chimanena kuti Zekariya amaonetsera dongosolo la Mulungu loumbanso Israeli kuti adzalandire Mesiya.

Anthu Ofunika: Zekariya, Yoshua wamsembe wamkulu.

Khristu mu Bukhu la Zekariya: Palibenso bukhu la mu chipangano chakale lomwe likukamba za umesiya loposa Zekariya. Bukhuli likukamba za mesiya kapena Khristu monga Mfumu komanso Mwana wa Mulungu, komanso monga Ngelo wa Ambuye (3:1), nthambi ya choonadi (3:8), mwala wa maso asanu ndi awiri (3:9), wakudzayo (12:10), mfumu yodzichepetsa (9:9-10), mbusa yemwe adzanyozedwe (13:7), ndi woweruza wakudzayo, komanso mfumu yachoonadi (14).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Pempho la Kulapa (1:1-6)**

2. **Masomphenya 8 a Zekariya (1:7–6:8)**
   a. Akavalo ndi okwera pa akavalo (1:7-17)
   b. Nyanga zinayi ndi amisili anayi (1:18-21)
   c. Akafukufuku (2:1-13)
   d. Yoswa ndi wansembe wamkulu (3:1-10)
   e. Choikapo nyali cha golide (4:1-14)
   f. Mpukutu wouluka (5:1-4)
   g. Mkazi ndi Efa (5:5-11)
   h. Magareta anai (6:1-8)

3. **Akorona a Yoswa (6:9-15)**

4. **Kusala Kudya, Kosalamulidwa ndi Yehova (7:1–8:23)**

7:1-7	8:9-13	8:20-23
7:8-14	8:14-17	
8:1-8	8:18-19	

5. **Kulangidwa kwa amitundu ena (9:1–14:21)**
   a. Kukanidwa kwa Mesiya (9:1–11:17)

9:1-10	10:1-12	
9:11-17	11:1-17	

   b. Ufumu wa Mesiya (12:1–14:21)

12:1-5	13:1-6	14:1-8
12:6-14	13:7-9	14:9-21

Malaki

(Kulapa ndi Kubwerera)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Malaki ndi yemwe watchulidwa monga mlembi wa bikhu la unenerili (1:1). Dzinaloti malaki limatanthauza "M'thenga Wanga." Izi zikuimilira kuti bukhuli unali uthenga wonenera za "kubwera kwa m'thenga wa pangano" (cf. 3:1), kulosera za Yohane mbatizi (Mateyu 11:10).

Zaka: 450-400 B.C. Pokhuzana ndi zakazi, mlembi wina wotchedwa Gleason Archier anati:

> kuyang'ana mkati mwakemo, zikuoneka kuti uneneriwu unanenenedwa mu zaka za mma 500 B.C., pafupifupi chaka cha 435 B.C. Tikudziwa izi chifukwa cha: (1) Kachisi anali atamangidwa kale ndipo nsembe ya mose itaperekedwa kale (1:7, 10; 3:1); (2) Kazembe wa a Peresi anali wolamulira pa nthawiyo, choncho siyinali nthawi ya ulamuliro wa Nehehemiya (445-433 B.C.);

> (3) Machimo omwe Malaki amatchula, anali omwe Nehemiya mu nthawi yachiwiri anawadzudzula monga, (a) kutailira kwa ansembe (1:6; Nehemiya 13:4-9), (b) kunyozera kupereka chakhumi, umphawi wa alevi (3:7-12 onananinso Nehemiya 13:10-13), (c) kukwatirana ndi amitundu (2:10-16, cf. Nehemiya 13:23-28). Ndi zanzeru kuti tidziwe kuti Malaki anali atadzudzula kale pa machimowo motsatira ndi Nehemiya, choncho chiyenera chinali chaka cha 435 B.C.[45]

Mutu ndi Cholinga: Pa utsogoleri wa Nehemiya panali chitsitsimutso (Nehemiya 10:28-39), koma ansembe ndi anthu analo ozizira pa kutsatira malamulo a Mulungu ngakhale anali ochimwa, Malaki anavumbulula ulesi, mphwayi ndi kunyozera chakhumi zomwe anthu ankachita molakwira mulungu. Ndipo malaki analemba yankho pa mafunso awo kwa ansembe ndipo izi zinaulula ndi kudzudzula uchimo wawo, ndipo mlaliki anamaliza ndi mawu a chilimbikitso a kubweranso kwa nthumwi ya Ambuye yemwe adzalambule njira ya Mesiya.

Ndipo Malaki anadzudzula anthu chifukwa cha kuleka kupembeza mulungu woona ndipo anakwatira ku kulapa. Mlembi wina, Gleason Archer anatsiriza za bukhuli motere:

> Cholinga cha bukhu la Malaki chinali kukhulupilira pamaso pa mulungu ndi makhalidwe oyera amoyo pamaso pa mulungu, kuti mulungu akondere mbewu zawo, dziko lawo, ndi kudalitsa chuma chawo. Israeli ayenera kukhala mu maitanidwe oyera ndikuyembekezera pa kudza kwa Mesiya yemwe adzatsogolere dziko kudzera mu utumiki wamachiritso ndi chiweruzo.[46]

Anthu Ofunika: Malaki

Khristu mu Bukhu la Malaki: Pokhuza za mesiya, alembic ena, Wilkison ndi Boa, anati:

> Bukhu la Malaki ndi lopsedera pa zaka 400 za kachetechete pa uneneri Wina, Yohane mbatizi ***"Ona mwana wankhosa wa mulungu amene achotsa uchimo wa dziko lapansi"*** (Yohane 1:29). Malaki akulosela kubwera kwa mthenga amene adzakonza njira Ambuye asanabwere (3:1 onani Yesaya 40:30). Patapita nthawi, Yohane M'batizi akukwaniritsa ulosi umenewu, koma mu ndime zotsatila (3:2-5), komanso anapita patsogolo ndikukamba za kubweranso kwachiwiri kwa Khristu.[47]

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Malo a Mtendere a Israeli (1:1-5)**
   a. Kulengeza chikondi cha Mulungu (1:1-2a)
   b. Adabwa chikondi cha Mulungu (1:2b)
   c. Chikondi cha Mulungu chaonekera (1:3-5)

2. **Kuonongeka kwa Israel (1:6–3:15)**
   a. Bodza (1:6-14)
   b. Kusakhulupirika (2:1-9)
   c. Maukwati osakanikirika (2:10-12)
   d. Kuthetsa maukwati (2:13-16)
   e. Kubwera kwa mnthenga (3:1-6)
   g. Umbava (3:7-12)
   h. Matama (3:13-15)

3. **Malonjezano a Mulungu pa Anthu (3:16–4:6)**
   a. Lonjezo la bukhu la chikumbutso (3:16-18)
   b. Lonjezo la kubwera kwa Khristu (4:1-3)
   c. Lonjezo la kubwera kwa Eliya (4:4-6)

Chaputala 3

Kafukufuku wa Mchipangano Chatsopano

Mau Oyambilira

Chipangano chatsopano ndi kulembedwa kwa kwa nkhani zokhudza mbiri ya uthenga wabwino. Zochitika za moyo opulumutsa Yesu Khristu moyo wake, imfa kuuka kukweera kumwamba ndi kupitiliza kwa ntchito yake mdziko lapansi kumene kukufotokodzedwa ndi Atumwi amene adawasakha ndi kuwatuma ku dziko lapansi ndikukukwanilitsidwa kwa zochitika zimene zayembekezeledwa nthawi yayitali ndichipangano chakale. Mopitilira, ndi "mbiri yoyeretsedwa" imene motsutsana ndi mbili yachikunja inalembedwa motsogozedwa ndi Mulungu izi zikutanthauza kuti monga chipangano chakale, ndichotetedzedwa ku zolakwitsa za munthu ndipo chili ndi ulamulilo wamphamvu ku mpingo walero komanso watsogolo kufikila Ambuye mwii adzabwerelenso.

Chiyambi ndi Tanthauzo la Chipangano Chatsopano: Baibulo lanthu, linagawidwa magawo awri Chipangano Chatsopano ndi Chipangano Chakale, koma zenizeni ndi zakuti izi zitathauzanji? Mawu a m'chigiliki a "chipangano amatanthauza" chifunilo, chipangano, kapena pangano." Chipangano Chakale kapena Chipangono ndi zolembedwa za Mulungu zoonetsa za ana a Israeli ndipo zikugwilitsa ntchito pangano la Mose lopatsidwa paphiri la Sinai. Chimodzimodzi chipangano chatsopano kapena pangano (loyembekedzeledwa mu Yeremiya 31:31 ndikukhazikitsidwa ndi mu 1 Akorinto 11:25) limafotokoza chikonzero chatsopano chatsopano cha Mulungu ndi munthu kuchokera ku mtundu uliwonse, ndi chilakhulo, ndi anthu ndi dziko amene adzamvomera chipulumutso atakhulupilira Khristu.

Chipangano Chakale, kunaululika chiyero cha Mulungu, muchoonadi chachilamulo ndiklonjeza momboli amene azadza chipano chatsopano chimaonetsa chiyero cha Mulungu mu chonadi chamwanayo, muomboli amene anadza mwa munthu. Chipangano chatsopano, chiri ndi zolembedwa zimene zimaulura uthunthu wa chipangano chatsopano.

Uthenga wa Chipangano Chatsopano wayika pa (1) Munthu amene adzadzipereka kukhulukira machismo (Mateyu 26:28) ndi (2) Anthu (mpingo) amene alandira chipulumutso chake. Apa ndiye pakati penipeni pa mut wa chipangano chatspano umene ndi "chipulumutso."[48]

Maina a pangano la kale ndi latsopano amagwilitsidwa ntchito pa mai wake awiri amene Mulungu analowamo ndi anthu, ndipo kenaka wamabuku amene analemba za ubale awiriwa. Chipangano cha Mulungu kudzera mmenemo watilandira iye kutendere ndi iye mwini.[49]

Kukonzekera kwa Uzimu za Chipangano Chatsopano: Munthawi ya Chiangano Chatsopano, Aroma anali mphamvu ndi ulamliro dzko lonse. Koma mdera laling'ono la Palestina-Beteli wa Yudea, mudabadwa iye amene adzasintha dziko lonsezokhudza ndi munthuyo mthumwi Paulo adalemba, ***"koma pamene kukwanila kwanthawi kunafika, Mulungu anatuma mwana wake, wobadwa mwa mzimayi, wobadwa pansi pa chilamulo"*** (i.e., pangano lakale) mumila zambili zapadera ndi njila zodabwitsa, Mulngu adakonzeratu njira ku dziko yakubwera Mesiya. Njira zambili zinathandizizila kukonzekeraku.

Kukonzekera Kudzera Fuko la Yuda: Kukodzekera kubwera kwa mesiya ndi nkhani ya chipangano chakale Ayuda adasakhidwa ndi Mulungukuchokera ku mafuko onse kuti akhale chuma chake, ngati ufumu wa ansembe ndi fuko loyera (Eksodo 1:5-6). Pamenepo, poyamba ndi malonjezano a Mulungu amene Mulungu anapeleka kwa a patiriak, Abrahamu, Isaki ndi Yakobo (Genesis 12:1-3; Aroma 9:4) amayenera kukhala osunga mau Mulungu (chipangano chakale [Aroma 3:2]) ndi mmene muli momboli (Genesis 12:2; Agalatiya 3:8; Aroma 9:5). Chipangano Chakale, choncho chinali chodzala ndi nkhani za kheistu ndi kuyembeza kubwera kwake ngati mpulumutsi ozudzidwa ndi olemekedzedwa mopitilira, kunalibe mauneneri ambiri, koma kunali nkhani zambili zopatsa chidwi zokhudza Mesiya kumene adzachokera, malo obadwira, zochitika mu nthawi ya kubadwa kwache, moyo, imfa ndi kuuka kwa akufa .

Ngakhale Israeli anali osamvera ndipo adatengedwa kuukapolo ngati chiweruzo chamulugu pa kulimbitsa mtima kwake. Mulungu, kenaka anabwerdzetsa otsulawo kuziko lawo patatha zaka 70, monga adalonjera pazakukonzekera kudzakwa Mesiya. Zaka four hundred zinali zitadutsa lachipangano chakale. Machitidwe a chipembezo ndiwo amene anadzetsa zikhupiliro zachilendo ndi chinyengo, koma panali mzimu woyembekezera meiya mmulengalenga ndi otsilira amadikira Mesiya.

Kukonzekera Kudzera Muchilankhulo cha Chigiliki: Ndizofonikila kwambili kuti Khristu adalumikiza omphunzila ake kupira kumapeto a dziko kukalalika (Mateyu 28:19-20) panali mau; "adziko lonse" izi zidali choncho chifukwa nkhondo ndi kufunitsitsa kwa Alexandr the Great mwana wa mfumu Philipi wa Macedon, amenezopambana 300 Khristu asanabadwe, anasesa dziko lonse pongonjetsa dziko. Chokhumba cha Alexander chiinali chilakhulo chimodzi ndi dziko limodzi, atatha ugojetsa anakhazikitsa chilakhulo cha cigiliki ngati chilakhulo chodziwiwka bwino ndi chikhalidwe cha chigiliki ngati chikhalidwe chokhazikika ndi moyo

umene anthu angamakhale. Ufumu wa Alexander unali wa nthawi yochepa koma zotsatira zofalitsa chilakhulo chachigiliki zidakhala kwa nthawi yayitali.

Nkhani ndiyakuti Mulungu anali Mulungu anali pa chintchitoyokodzekeretsa dziko ndi chinenedwe chomveka bwino chodziwika kwa anthu. Chilankhulochi chinagwilitsidwa ntchito yolalikira uthenga wampulumutsi. Zotsatira zake mabuku achipangano chatsopano analembedwamuchilankhulo cha pnseponse munthawi sizinalembedwe mu chiheberi kapena mu arebic. Ngakhakle kuli olemba onse a Yuda kupatulura Luka, wamtundu. Chigiliki chidakhala chilakhulo chachiwiri kwa aliyense muziko loziwika lnthawi imeney.

Kukonzekeretsedwa Kudzera kwa Aroma: Murungu sanamalize kukonzekeletsa dziko pazakubwera kwa mpulumutsi wa dziko Yesu adabadwa ku Palestine, aroma anaramula dziko lonse. Palestine anari pansi pa ulamuriro w aroma pamwamba zonse. Roma adadziwika ndi kurimbikitsa kwake chilamuro ndi ndondomeko nkhondo ya pa chiweniweni imene anthu adakhetsa mwazi mumbiri t aroma inafika kumapeto ndi uramuliro wa kaisara augustus zosarira zake, nkhondo imene idatenga zaka 100 inafika kumapeto ndipo roma adakuzidwa malire ake. Aroma adamanganso misewu imene imatetezedwa ndi guru la ankhondo ake, zimene zidazetsa bata ndi mtendere kwa onse oyenda mmisewuyi kulowa ndi kuturuka munzindawu mfumu imeneyi augustus Ceasar inari yoyamba kuvara zovara zofiira ndi duwira ngati mfumu yokhayo ya mzindawo inali ya nzeru ndi yoganiza anthu ake, ndipo inazetsa nthawi zantengo wapatari za mtendere ndi kulemera Roma adapangidwa mzinda wapamwamba okoma kukhara ndi kuyendamo izi zidabweretsa nthawi yotchedwa “Pax Romana” mtendere w Aroma (27 B.C.–A.D. 180) ndiye chifukwa cha zonse zimene augustus anachita, amisiri anari mmene iye anabada, “Mulungu adabadwa” unary mtendere weniweni ofika munthawi yake komanso okhazikika padziko lonse chimodzimodzi Yesu anali murungu oona obadwa mwa munthu mmaro mwamunthu adaphedwa murungu kupezeka kwa uramurilo w Aroma ndi chilamuro zidathandiza kukonzekeretsa dziko lonse za moyo wake ndi utumiki kuti uthenga ukalalikiridwe .

Dziko la Chipembezo Munthawi ya Chipangano Chatsopano: Tisanafufuze chipangano chatsopano–zithandiza kukhara ndi lingarilo ndi ganizo la dzikola chipembedzo pamene mpulumutsi adadza ndipo kenaka ndikutumampingokudzikolonse mukamawerenga mawu a mmusiwa ochokera kwa Merrill C. Tenney muyang anekufanana kwake ndi dzikolathu lero.

Mfundo 2: Ndondomeko zikufunika zichokere mu chiphunzitso choyenera komanso chiphunzitsochi chichokere mu mawu a Mulungu ndi kuphunzitsidwa ndi anthu auzimudi (2 Timoteo 2:15). Cholinga cha Mulungu cha choonadi, kuphatikizapo uzimu wa munthu wophunzitsa mawu (1 Timoteo 3:1-10), ndizofunika kwambiri pofuna kumanga mpingo wathanzi. Pamene okhulupilira amanga ndikuyendetsa mpingo papanda zomwe talongosolazi, mapeto ake umangokhala mpingo wopanda chauzimu chirichonse ndi wakufa mu zonse. Ma Bukhuwa akulongosola ndondoeko ya momwe mpingo uuyenera kuyendetseredwa ndondomeko yomwe siyinalongosolepo mu mabukhu ena. Poyamba, asanapereke dongosololi, anapereka mabukhu awa: Aroma, 1 ndi 2 Akorinto, Agalatiya, Aefeso, Afilipi ndi Akolose.

Mabukhuwa amakalata, amaoneka ngati ofanana, komabe amasiyana mu zolinga motere:

Chidzindikizo pa Ambuye Yesu Khristu	
Aroma	Khristu, Mphamvu ya Mulungu kwa anthu
1 Akorinto	Khristu, Nzeru za Mulungu kwa anthu
2 Akorinto	Khristu, Chitonthozo cha Mulungu kwa anthu
Agalatians	Khristu, Choonadi cha Mulungu kwa anthu
Aefeso	Khristu, Ulemelero wa Mulungu kwa anthu
Afilipi	Khristu, Chidzalo cha Mulungu kwa anthu
Akolose	Khristu, Chikhutitso cha Mulungu kwa anthu
1 Atesalonika	Khristu, Lonjezo la Mulungu pa anthu
2 Atesalonika	Khristu, Dipo la Mulungu pa anthu
1 Timoteo	Khristu, Mkhalapakati wa Mulumgu pa anthu
2 Timoteo	Khristu, Woweruza wa Mulungu pa ife
Tito	Khristu, Kukoma mtima kwa Mulungu pa anthu
Filimoni	Khristu, Chikhulupiliro cha Mulungu pa anthu

Kutsindika Pa Uthenga Wabwino	
Aroma	Uthenga Wabwino ndi uthenga wake
1 Akorinto	Uthenga Wabwino ndi Utumiki wake
2 Akorinto	Uthenga Wabwino ndi Atumiki ake
Agalatiya	Uthenga Wabwino ndi Kukhadzula/Kunena Chindunji kwake
Aefeso	Uthenga Wabwino ndi nkhani Zakumwamba
Afilipi	Uthenga Wabwino ndi nkhani Zapansi Pano
Akolose	Uthenga Wabwino ndi nzeru za Kaganizidwe ka Anthu
1 Atesalonika	Uthenga Wabwino ndi tsogolo la Mpingo
2 Atesalonika	Uthenga Wabwino ndi za wokana Khristu
1 Timoteyo	Uthenga Wabwino ndi Abusa ake
2 Timoteyo	Uthenga Wabwino ndi Chitsutso
Tito	Uthenga Wabwino ndi Kalongosoledwe kake
Filemoni	Uthenga Wabwino ndi Kulungama kwake

Chitsimikizo cha Uthenga Wabwino pa Umodzi wa Okhulupilira	
Aroma	Mwa Khristu muli Chilungamo
1 Akorinto	Mwa Khristu muli Kuyeretsa
2 Akorinto	Mwa Khristu muli Chitonthozo
Agalatiya	Mwa Khristu muli Chiyanjano
Aefeso	Mwa Khristu muli Kukwezedwa
Afilipi	Mwa Khristu muli Ichimwemwe
Akolose	Mwa Khristu muli mathero
1 Atesalonika	Mwa Khristu muli Mathero
2 Atesalonika	Mwa Khristu muli Chipepeso
1 Timoteo	Mwa Khristu muli Chikhumbokhumbo
2 Timoteo	Mwa Khristu muli Chitsimikiziro
Tituo	Mwa Khristu muli Machawi
Filimoni	Mwa Khristu muli Chidwi

Aroma

(Khristu: Mphavu ya Mulungu pa Anthu)

Mlembi ndi Dzina La Bukhu: Monga kalata bukhuli likufotokozera kuti, Paulo ndiye mlembi wa bukhuli (1:1). Kalatayi ikulongosola nkhani zambiri zomwe zinamuchitikira Paulo mu moyo wake koma chiphunitso chowe chiri mu kalatayi ndi chofnana ndi akalata ena.

Bukhu la Aroma, lomwe limachulidwa “Ntchito zazikulu za Paulo” ndipo dzina la bukhuli lachokera pachifukwa choti imalemberedwa ku mpingo wa ku Roma koma monga mtuwi wa amitundu anakhala akufunisitsa kuti akawayendere okhulupilira aku Roma (15:22-23) kuti akawathandize kukhazikika mu chikhulupiliro ndi kulalikira uthenga bwino (1:13-15).

Pokhumbitsitsa kukalalikira ku Aroma Paulo analembera kalatayi pamene pamene anali kukonzekera ulendo wokawachezera (15:14-17). Analemba kalatayi ali ku Akorinto pomwe amatolera chopereka chothandizira osowa aku Palestina. Kuchoka apo anapitanso ku Yerusalemu kukatula ndalama pofuna kupitilira ku Roma ndi

Spain (15:24). Paulo anapereka ku Roma, monga wa ndende. Ndipo zikuoneka kuti Febe anali yemwe amapephera ku mpingo wa ku Cenchrea pafupi ndi Korinto (16:1), ndiyewe anatenga kalatayi.

Zaka: A.D. 57–58 Bukhuli linalembedwa mu A.D. 57–58 pafupi ndi nthawi ya ulendo wake wachitatu (Machitidwe 18:23–21:14; Aroma 15:19). Malinga ndi zomwe analemba mu Aroma 15:26, zikuoneka kuti munthawiyi Palo anali atalandira chopereka kuchokera ku Makedonia ndi Achaia (ku Akorinto). (cf. 1 Akorinto 16:1-4; 2 Akorinto 8–9), zolembazi zatsogozana ndi 1 ndi 2 Akorinto lomwe linalembedwa mu A.D. 55.

Mutu ndi Cholinga: Kalatayi siinalembedwa pofuna kuthana ndi mavuto ena monga achitira makalata ena. Pali zolinga ziatatu zimene zikuoneka pamene kalatayi imalembedwa: **choyamba:** Kufuna kulengeza za ulendo wa Paulo wopita ku Roma, atatha ulendo wake wobwerera ku Yerusalemu pamene amakonzekeranso mpingo pa kubwera kwake (15:24, 28-29 cf. Machitidwa 19:21). Paulo amafuna kuwadziwitsa za ulendo wake komanso kuwauza zoti iwo akonzekere komanso kupempherera kuti izi zikwaniritsidwe. (15:30-32). Cholinga **chachiwiri:** ndichakuti Paulo amafuna kupereka uthenga wabwino komanso wokwanira bwino umene Mulungu wamuitanira. Iye monga mtumwi sankangofuna kuti ***"akangolalikira uthenga kwa Aroma"*** (1:15), koma amafunanso alongosole bwino za tanthauzo ndi kukula kwa zinthu zokhudza moyo, kuphatikizapo kale: (kulungamitsidwa kumene kukumupangitsa wina kukhala wolungama), zatsopano; (kuyeretsedwa kuemene kukutanthauza kupatulidwa), ndi zinthu zamtsogolo; (kulandira ulemelero zimene zikutatanthauza kugawana ndi Khristu ulemelero). **Cholinga chachitatu**: ndichakuti Paulo amalembanso poyankha funso lomwe linali pakati pa Ayuda ndi aKhristu amitundu okhala ku Roma; funso lake linali: *Kodi uthenga wabwino umachita chiyani ku chilamulo monga za mdulidwe wa kuchipangano chakale? Kodi nanga ayuda, Mulungu wawapatula okha basi?kapena Mulungu waiwala pangano lake kwa aYuda?* Paulo anayankha mafunsowa polongosola dongosolo la Mulungu pa Ayuda ndi Amitundu.

Mutu weniweni mu Aroma uli pa 1:16-17. Pomwe mtumwi akutionetsera momwe Mulungu amapulumutsira anthu ochimwa. Mu mavesi awa, muli mitu yeniyeni ya kalatayi monga: uthenga wabwino, mphamvu ya Mulungu, chipulumutso, yense wokhulupilira, chilungamo mwa Mulungu, ayuda ndi amitundu. Charles Ryrie anafotokoza bukhu la Aroma motere:

> Kuposa makalata ena a Paulo, Aroma akulongosola chiphunzitso cha kulungamitsidwa mwa chikhulupiliro monga njira yoyenerera. Mutu wa kalatayi ndi chilungamo cha Mulungu (1:16-17). Komabe bukhuli lalembanso nkhani zina monga: bvumbulutso (Aroma 1:19-20), kufanana kwa tchimo (Aroma 2:9-20), kulungamitsidwa (Romans 3:24), kugawikana (Aroma 3:25), chikhulupiliro (Aroma 4:1), tchimo loyamba (Aroma 5:12), umodzi mwa Khristu (Aroma 6:1), kusankhidwa ndi kukanidwa kwa Israyeli (Aroma 9–11), mphatso za Mzimu (Aroma 12:3-8), kupereka ulemu ku boma ndi kwa olamulira (Aroma 13:1-7).[73]

Kupatulapo malonje (1:1-17) ndi ndemanga (15:14–16:27), Kalata ya Aroma yagawidwa magulu atatu:

1. Machaputala 8 oyambirira ndi a **chiphunzitso,** cha chiyero (kulungamitsidwa ndi kuyeretsedwa) kudzera mu chikhulupiliro pa Mulungu.
2. Ma chaputala atatu otsatirawo (9–11) ndi a **dziko,** ndipo akulongosola zokhuza Mulungu pa ayuda ndi amitundu polumikizana ndi uthenga wabwino.
3. Ma chaputala othiriza (12–16) akulongosola **ntchito zoyenera kuzigwira** munthu wokhulupilira Mulungu, pa tsiku lirilonse la moyo wake.

Khristu mu Bukhuli: Paulo akulongosola Yesu Khristu monga Adamu wachiwiri yemwe imfa yake ya chilungamo ndi yoimilira anthu, yabweretsa kulungama kwa anthu onse okhulupilira mwa iye Iye akupereka chilungamo monga mphatso ya chisomo kwa munthu wopanda chimo, yemwe wasiya zoipa zones za padziko. Imfa ndi kuukitsidwa kwa Yesu ndiwo maziko a chiombolo, chilungamo, kubwezeretsedwa, ulemelero ndi kukwezedwa kwa okhulupilira.[74]

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Malonje (1:1-17)**
   1:1-7 1:8-15 1:16-17

2. **Chidzudzulo: Kufunikira kwa Choonadi (1:18–3:20)**
   a. Chidzudzulo pa anthu amitundu (1:18-32)
      1:18-23 1:24-27 1:28-32
   b. Chidzudzulo pa ntchito zathupi (2:1-16)
      2:1-11 2:12-16
   c. Chidzudzulo pa Ayuda (Anthu opemphera) (2:17–3:8)
      2:17-24 2:25-29 3:1-8

d. Chidzudzulo kwa anthu onse (3:9-20)
3:9-18 3:19-20

3. Kulungamitsidwa: Choonadi cha Mulungu mwa Khristu Yesu (3:21–5:21)
a. Choonadi (3:21-31)
3:21-26 3:27-31
b. Dongosolo la choonadi (4:1-25)
4:1-8 4:13-15
4:9-12 4:16-25
c. Madalitso pa kukhala mu choonadi (5:1-11)
d. Kusiyana kwa choonadi ndi Chidzudzulo (5:12-21)
5:12-14 5:15-17 5:18-21

4. Chiyero: Choonadi Chikufalitsidwa ndi Kuonetseredwa (6:1–8:39)
a. Chiyero ndi Uchimo (6:1-23)
6:1-7 6:12-14 6:20-23
6:8-11 6:15-19
b. Chiyero ndi Chilamulo (7:1-25)
7:1-3 7:7-13 7:21-25
7:4-6 7:14-20
c. Chiyero ndi Mzimu Woyera (8:1-39)
8:1-8 8:18-25 8:28-30
8:9-17 8:26-27 8:31-39

5. Kuonetsa Poyera: Ayuda ndi Amitundu-Kawuni-uni wa Choonadi (9:1–11:36)
a. Israeli m'nthawi yakale: Chisankho cha Mulungu (9:1-29)
9:1-5 9:14-18 9:27-29
9:6-13 9:19-26
b. Israeli nthawi ino: Kukanidwe ndi Mulungu (9:30–10:21)
9:30-33 10:5-13 10:16-17
10:1-4 10:14-15 10:18-21
c. Tsogolo la Israeli: Kubwezeretsedwa ndi Mulungu (11:1-36)
11:1-6 11:11-16 11:25-32
11:7-10 11:17-24 11:33-36

6. Mapangidwe: Kukhala mu Choonadi (12:1–15:13)
a. Mu ubale ndi Mulungu (12:1-2)
b. Mu ubale ndi anthu ena (12:3)
c. Mokhudzana ndi mpingo (12:4-8)
d. Pokhala mu dera (12:9-21)
12:9-13 12:14-21
e. Kwa olamulira (13:1-14)
13:1-7 13:8-10 13:11-14
f. Kwa aKhristu ena (14:1–15:13)
14:1-4 14:10-12 15:1-6
14:5-9 14:13-23 15:7-13

7. Uthenga wa Paulo ndi Pemphero la Mdalitso (15:14–16:27)
a. Malingaliro a Paulo (15:14-33)
15:14-21 15:22-29 15:30-33
b. Uthenga wa Moni wa Paulo (16:1-16)
16:1-2 16:3-16
c. Mathero ndi Mdalitso (16:17-27)
16:17-20 16:21-24 16:25-27

1 Akorinto

(Khristu: Nzeru ya Mulungu pa Anthu)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Paulo ndiye mlembi wa bukhuli malinga ndi zomwe zalembedwa mu kalatayi. Clement wa ku Rome (mbusa wa mu zaka za A.D. 200) analemba kuti 1 Akorinto ndi "Kalata ya mtumwi Paulo Wodala" chifukwa cha momwe Paulo analembera kalatayi (1:1; 16:21 cf. 1:12-17; 3:4, 6, 22).

Mu bukhu la Machitidwe a Atumwi ndi mumakalata ena akulongosolanso za mpingo wa ku Akorinto ndipo Paulonso akutchulidwamo mu nkhani zambiri: (1) ulendo wake ku Akorinto, motsatizidwa ndi (2) kalata yake yoyamba yaku Akorinto (yomwe inasokonekera), (3) kalata yake yachiwiri yopita ku Akorinto (1 Yomwe ndi 1 Akorinto, lero), (4) ulendo wake wa ku Akorinto ("ulendo wowawa," 2 Akorinto 2:1), (5) kalata yachitatu yaku Akorinto (yomwe inatayika). Yomwe inatsatiridwa ndi 2 Akorinto, (6) kalata yachinayi ku Akorinto, (7) ulendo wake wachitatu wa ku Akorinto (Machitidwe 20:2-3). Tiyenera kudziwa kuti makalata awiriwo amene anataika anagwirizana ndi cholinga cha Mulungu kuti asakhale mbali imodzi ya mabuku ovomerezedwa.

Zaka: A.D. 55 Paulo anayamba kulalikira ku Akorinto pa ulendo wake wachiwiri umene unali mu A.D. 50. Pamene iye anali kumeneko anagwira ntchito ndi Akula ndi Priscilla omwe anali osoka ma hema (Machitidwe 18:3). Paulo analalikira mu Sunagoge koma anathamangitsidwa ndi aYuda omusutsa. Komabe iye anapita khomo loyandikana nalo la Titiyasi Yusto kumene iye anapitiliza utumiki wake (Machitidwe 18:7). Ngakhale analandira chitsutso kwa aYuda kudzera mwa chiwanga cha Chiroma wotchedwa Gallio, Paulo anakhalabe miyezi 18 ku Akorinto (Machitidwe 18:1-17; 1 Akorinto 2:3). Kalatayi inalembedwa chaka cha A.D. 55 (16:5-9; Machitidwe 20:31). Kuchokera ku umboni wake kuti anakhala ku Aefesokufikira pentekoste (Machitidwe 16:18), zikuoneka kuti iye amafuna kukhala komweko kwa nthawi yosapitilira chaka pamene analemba kalata wake woyamba.

Mutu ndi Cholinga: Pofuna kumvesetsa cholinga ndi mutu, pakufunika kudziwa za mbiri pang'ono. Korinto unali mzinda wa anthu pafupifupi 700,000, ndipo pafupifupi gawo limodzi mwa magawo atatu anali akapolo omwe ankakhala pakachilumba paakati pa Nyanja ya Aegean ndi Adriatic yomwe inalumikiza Peloponnesus ndi kumpoto kwa Greece. Ndipo ngakhale analemera, mu kuona kwa umunthu, Paulo ndi anzake ena anaganiza kuti ndi uthenga wanji wabwino womwe ungakhale mu mzinda wa Korinto. Monga mzinda, unali ndi mbiri ya uchimo ndi kukhulupilira zathupi. Mzindawu unadzazidwa ndi tiakachisi ta timilungu ta Aphrodite tomwe tinali pamwamba 1800-ft (550 mamita) kutalika kwake, otchedwa ma Acrocorinthus. Mu mayambiliro a zilembo za chigiriki, zimalumikizidwa ndi ntchito zathupi. Mawu oti, "Mtsikana wa ku Korinto'' ankatanthauza 'Hule,'' ndipo mawu oti "zochita za akorinto,'' amatanthauza "chigololo." Chuma chambiri ku Korinto chinazungululidwa ndi tiakachisiti ndi azimayi achigololo. Pa chifukwa ichi, mwambi umawachenjeza kuti'si mwamuna aliyense akhale wotengeka ndi zakukorinto.

Kudzera mu za mu Machitidwe a Atumwi, zikuoneka kuti Paulo akadakhala ndi otembenuka mtima ochepa a Chiyuda, komabe ochuruka a iwo otembenuka mtima anali amitundu. Anthu amenewa anali ochokera ku maudindo ang'ono ang'ono, ngakhale ena amaonekanso kuti ali ndi amaudindo akulu (1:26-31). Komabe pamaoneka kusiyana pa khalidwe komanso pa chuma pakati pawo (7:20-24; 11:21-34). Anthu amenewa anali ndi maonekedwe achikhalidwe ndi zokhudza chuma zimene zimawasiyanitsa (7:20-24,11:21-34); enanso anali anthu amene amapanga makhalidwe achikunja (6:9-11). Pomwe monga aGiriki ankazitamandira okha kuti ndiwo anzeru, ngakhale kuti mu nthawi imeneyi izi zinali zitachepa (1:17; 2:1-5).[75]

Ndipo anthu akhonza kuona kuti chikhalidwe choipa cha chipembedzo ndi chachitaiko chaononga bwanji mpingo ku moyo wauzimu ndi chikhalidwe. Mutu wa bukhu limeneli ndi lokamba za m'mene moyo watsopano waChikhristu, woyeretsedwa ndi Khristu ndi maitanidwe a onse oyera mtima, ukhale pa zochitika zonse za moyo wathu. Moyo watsopano umeneu mwa Khristu ukutiitanira ife ku moyo watsopano mwa Mzimu Woyera (3:16, 17; 6:11, 19-20). Malingaliro a Mulungu ndi ofuna kusintha okhulupilira ku thupi ngakhalenso kuuzimu.

Bukhuli linalembedwa poyankha ndi kuphunzitsa kuti pakhale kulongosoka pa mpingo ndi okhulupilira (1:21-30), zachisawawa (5:1-13; 6:9-20), ndi kuyankha mafunso okhuza ukwati, kuthetsa ukwati, chakudya, mapembezedwe, mphatso za mzimu ndi kuuka kwa kufa. Ndipo mafunsowa amafunsidwa chifukwa anthu ambiri a mudzikoli anali osatembenuka mtima.

Khristu mu Bukhuli: Mu 1:30, akuti ***"kudzera mu ntchito zake, muli mwa Khristu Yesu, yemwe anakhala mzeru yochokera kwa Mulungu ndi choonadi ndi chiyero ndi chiombolo."***

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Chiyambi (1:1-9)**
   a. Malonje (1:1-3)
   b. Pemphero la chiyamiko (1:4-9)

2. **Malekano mu Mpingo (1:10–4:21)**
   a. Magawano (1:10-17)
   b. Zifukwa za magawano (1:18–2:16)

1:18-25	2:1-5
1:26-31	2:6-16

c. Zotsatira za Magawano (3:1–4:5)

3:1-4	3:10-15	3:18-23
3:5-9	3:16-17	4:1-5

d. Paulo awonetsa Chitsanzo (4:6-21)

4:6-7	4:8-13	4:14-21

3. Za Chisawawa mu Mpingo (5:1–6:20)

a. Tchimo la Chigololo (5:1-13)

5:1-5	5:6-8	5:9-13

b. Mirandu pakati pa abale (6:1-8)

c. Awachenjeza adane nalo tchimo (6:9-20)

6:9-11	6:12-20

4. Malangizo a za Ukwati (7:1-40)

a. Ukwati ndi Umbeta (7:1-9)

b. Ukwati ndi chilekaniro pa Ukwati (7:10-24)

7:10-11	7:17-20
7:12-16	7:21-24

c. Ukwati ndi kutumikira Mulungu (7:25-38)

7:25-31	7:32-35	7:36-39

d. Ukwati, kutha ukwati, ndi kukwatiranso (7:39-40)

5. Malangizo a Kudya Zoperekedwa kwa Mafano (8:1–11:1)

a. Funso: Kodi munthu azidya chakudya choperekedwa kwa Mafano? (8:1-13)

8:1-3	8:4-6	8:7-13

b. Chitsanzo cha Paulo (9:1-27)

9:1-2	9:8-14	9:19-23
9:3-7	9:15-18	9:24-27

c. Malangizo (10:1–11:1)

10:1-5	10:14-22	10:31-33
10:6-13	10:23-30	11:1

6. Malangizo a za Kupembeza Mumabwalo (11:2–14:40)

a. Zoyenera Akazi (11:2-16)

b. Machitidwe a Mgonero wa Ambuye (11:17-34)

11:17-22	11:27-32
11:23-26	11:33-34

c. Ntchito za mphatso za Mzimu Woyera (12:1–14:40)

12:1-3	13:1-3	14:13-19
12:4-11	13:4-7	14:20-25
12:12-13	13:8-13	14:26-33
12:14-26	14:1-5	14:34-36
12:27-31	14:6-12	14:37-40

7. Za Kuuka kwa Kufa (15:1-58)

a. Phindu lakuuka kwa kufa (15:1-11)

15:1-2	15:3-11

b. Zotsatira za kukana Chiukitso (15:12-19)

c. Chiyembekezo cha MKhristu (15:20-34)

15:20-28	15:29-34

d. Kuukitsidwa kwa thupi (15:35-50)

15:35-41	15:42-50

e. Chipambano cha okhulupilira (15:51-58)

15:51-57	15:58

8. Zopereka za kwa Anthu aku Yerusalemu (16:1-4)

9. Mathero (16:5-24)

16:5-9	16:13-14	16:21-24
16:10-12	16:15-20	

2 Akorinto

(Khristu: Mtonthozi Wathu)

Mlembi ndi Dzina la Bukhuli: Paulo ndiye mlembi wa bukhuli. Pali umboni wa mkati ndi kunja wosonyeza kuti Paulo ndiye mlembi wa bukhuli. Bukhuli lalembedwa mu kalembedwe koonetsa m'mene Paulo amalembera komanso likufotokoza za moyo wake kusiyana ndi mabukhu ena onse.[76]

Zaka: A.D. 56 Chifukwa cha chisokonezo cha wosula tiakachisi ta siliva (Machitidwe 19:23-41), Paulo anawathawira ku Aefeso ndipo anapita ku Makedonia (Machitidwe 20:1). Mu nyengo ya chilimwe mu A.D. 56. Ali paulendowu, anaima pa Trowa kuti akumane ndi Tito (2 Akorinto 2:13) ndi kulandira uthenga wa mmene zinthu ziriri kwa anthu ochokera ku mpingo waku Akorinto. Popeza sanathe kukumana naye Tito, Paulo anapitilira ku Makedonia, ali ndi chikhumbokhumbo chofuna kukumana naye Tito kuti atetezedwe (2 Akorinto 7:5-6). Ndipo kumeneko anakumana naye Tito yemwe anabweretsa uthenga wokoma wa ku Akorinto ndi wina woipa woti gulu lina la anthu amatsutsana ndi chiphunzitso ndi utumwi wa Paulo Mtumwi. Kuchokera ku Makedonia, Paulo analemba makalata anayi, kuphatikizapo 2 Akorinto. Paulo anapitilira ulendo wake, wachitatu ku Akorinto mu nyengo yachisanu ya A.D. 56-57 (Machitidwe 20:2-3).

Mutu ndi Cholinga: Mwa makalata onse a Paulo, 2 Akorinto ndi yomwe analemba motsindika. Kudzera mu kalatayi, anatsegula mitima ya anthu ndikuwalimbikitsa kuti akhale angwiro mu chikondi ndi machawi. Koma James K. Lowery analongosola mu "the Bible Knowledge Commentary":

> Zomwe zinamukhudza Paulo zinali za chiphunzitso cha aphunzitsi onyenga, ozitzhula okha Atumwi, omwe amapezeka mu mpingo. Anthu oterewa amapha ndi kunyozetsa mbiri yabwino ya chiKhristu ndi uthenga wa Atumwi. Paulo anadziwa kuti ndi kofunika kuti apereke uthenga wa chilimbikitso ku mpingo kuti utsutsane ndi khalidwe loipali.[77]

Mu chodzikanira chake, Paulo panaonekera zolinga zake zitatu: (1) Paulo analongosola za chimwemwe chake ndi m'mene mpingowu unalandilira chiphunzitso chomwe iye anaphunzitsa (1:1–7:16); (2) Amawakumbutsa okhulupilira kuti apitilire kusonkha chopereka cha okhulupilira aku Yudea (8:1–9:15); ndi (3) Amalemba pofuna kuteteza ulamuliro ndi chiphunzitso cha Utumwi (10:1–13:14).

Khristu mu Bukhuli: Mu bukhuli, tikuona Khristu monga Mtonthozit (1:5), chimwemwe (2:14), Ambuye (2:4), Ufulu pa moyo watsopano (3:17), kuunika (4:6), woweruza mwacghilungamo (5:10), wobwezeretsa ndi kukhululukira (5:19), mphatso (9:15), Mwini (10:7) ndi mphamvu (12:9).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule[78]

1. **Makhalidwe a Paulo pa Ntchito ya Utumwi (1:1–7:16)**
   a. Malonje (1:1-2)
   b. Chiyamiko pa chitonthozo cha Mulungu (1:3-11)
      1:3-7 1:8-11
   c. Chiyero cha ntchito ndi malingaliro a Paulo Mtumwi (1:12–2:4)
      1:12-14 1:23-24
      1:15-22 2:1-4
   d. Kukhululukira okhumudwitsa a ku Korinto (2:5-11)
   e. Utsogoleri wa MMulungu mu utumiki (2:12-17)
      2:12-13 2:14-17
   f. Okhulupilira a ku Korinto–Kalata yochokera kwa Khristu (3:1-11)
      3:1-3 3:4-11
   g. Kuona ulemerero wa Mulungu wa Mulungu (3:12–4:6)
      3:12-18 4:1-6
   h. Chuma mu Mbiya za dothi (4:7-15)
      4:7-12 4:13-15
   i. Paulo alalikira Khristu yekha yekha (4:16–5:10)
      4:16-18 5:1-5 5:6-10
   j. Utumuki wa kuyanjananso (5:11–6:10)
      5:11-15 5:20-21
      5:16-19 6:1-10
   k. Tate muuzimu awadandaulira ana ake (6:11–7:4)
      6:11-13 7:1
      6:14-18 7:2-4
   l. Paulo akondwera ndi kudza kwa Tito (7:5-16)
      7:5-12 7:13-16

2. **Chikhumbo-Khumbo: Mkumano wa Akhristu ku Yerusalemu (8:1–9:15)**
   a. Kupatsa aumphawi (8:1-15)
      8:1-6 8:7-15
   b. Tito ndi anzake atumizidwa ku Korinto (8:16–9:5)
      8:16-24 9:1-5
   c. Zotsatira za kupereka kwa osowa (9:6-15)

3. **Umboni wa Paulo pa Ntchito ya Utumwi (10:1–13:14)**
   a. Ulamuliro wa Paulo Mtumwi (10:1-18)
      10:1-6 10:7-11 10:12-18
   b. Paulo anena za Atumwi onyenga (11:1–12:21)
      11:1-6 11:21-29 12:11-13
      11:7-11 11:30-33 12:14-18
      11:12-15 12:1-6 12:19-21
      11:16-20 12:7-10
   c. Machenjezo omaliza (13:1-10)
      13:1-4 13:5-10
   d. Mathero (13:11-14)

Agalatiya

(Khristu: Chilungamo cha Mulungu pa Anthu)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Paulo akudzionetsa yekha monga mlembi wa bukhuli, "kalata ya Paulo Mtumwi yolembera ku Agalatiya."

Zaka: A.D. 49 Kalatayi inalemberedwera aKhristu a ku M'wera kwa Agalatiya. Mipingoyi inayambitsidwa ndi Paulo pa nthawi ya maulendo ake. Kalatayi inalembedwa kumapeto kwa ulendo wake woyamba, pafupifupi mu chaka cha A.D. 49, ndipo zikusonyeza kuti iyi inali kalata yoyambrira ya Paulo, utangotha mkumano wa ku Yerusalem (Machitidwe 15).

Mutu ndi Cholinga: Kalata ya Paulo ku Agalatiya imatchulidwanso ndi ophunzira mau a Mulungu kutu "Chikalata cha Ufulu wa Chikhristu." Aalatiya anali anthu ozikika pa zachiyuda, zomwe zimaphunzitsa za chilamulo cha dziko osati zokhuza chisomo cha Mulungu. Mwa zina, iwo anaphunzitsa miyambo yachikhalidwe yak u chipangano cha kale, mumpingo. Mtumwi Paulo anawalembera kalata yosutsana nawo izi ndi kuwaunikira ukulu, ndi chilungamo mwa chikhulupiliro ndi chiyeretso cha Mzimu woyera.

Poonjezera apo, chikhalidwe cha chiYudachi chimaphunzitsa uthenga wabodza, komanso wonyoza utumwi ndi ziphunzitso za Paulo. Mu machaputala oyambirira, Paulo akuchinjiriza utumwi wake ndi uthenganso womwe anaulandira mwa bvumbulutso kuchokera kwa Khristu Yesu. Ndipo mu chaputala 3 ndi 4 iye akulongosola za chiphunzitso choona, cha chilungamo mu chikhulupiliro, komabe akulongosola za ufulu wa Akhristu, ndi kudana nditchimo. Mu chaputala 5 ndi 6 akuonetsa kuti Akhristu ayenera aphunzire kukhala mu mphamvu ya Mzimu, Mzimu womwe ungaongolere mayendedwe awo ndi kuchitira umboni osati mu ntchita za thupi, koma monga zipatso za mzimu.

Khristu mu Bukhuli: Kudzera mu imfa yake, okhulupilira onse anafa muchilamulo ndi kuukanso mwa Yesu Khristu (2:20). Okhulupilira amasulidwa ku nsinga (5:1f.) ndipo apatsidwa ufulu. Mphamvu ya mtanda imapereka chiombolo kuchoka ku temberero la chilamulo, kuchoka ku mphamvu ya chimo (1:4; 2:20; 3:13; 4:5; 5:16, 24; 6:14).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Maganizo: Uthenga Wabwino wa Chisomo, Achinjiriza Chilungamo mu Chikhulupiliro (1:1–2:21)**
   a. Malonje (1:1-10)
      1:1-2 1:3-5 1:6-10
   b. Uthenga wabwino wa Chisomo, unabwera mu Bvumbulutso (1:11-24)
      1:11-12 1:13-17 1:18-24
   c. Uthenga wabwino wa Chisomo unavomerezedwa ndi mpingo wa ku Yerusalemu (2:1-10)
   d. Uthenga wabwino wa Chisomo unaonetsedwa pa chidzudzulo cha Petro (2:11-21)
      2:11-14 2:15-21

2. **Chiphunzitso: Uthenga wabwino wa Chisomo, Chilungamitso mwa chikhulupiliro chilongosoledwa (3:1–4:31)**
   a. Zomwe anaziona Agalatiya: Mzimu waperekedwa mwa Chikhulupiliro (3:1-5)
   b. Chitsanzo cha Abrahamu: Iye analungamitsidwa mwa chikhulupiliro, osati mwa ntchito (3:6-9)
   c. Munthu adzalungamitsidwa mwa chikhulupiliro, osati mwa chilamulo (3:10–4:11)

3:10-14	3:19-22	4:1-7
3:15-18	3:23-29	4:8-11

   d. Agalatiyaanalandira Madalitso mwa chikhulupiliro,osati mwa chilamulo (4:12-20)
   e. Chilamulo ndi Chisomo ndi zinthu zosiyana (4:21-31)

3. **Zochitika: Uthenga wabwino wa Chisomo, Alungamitsidwa mwa chikhulupiliro (5:1–6:18)**
   a. Maimidwe a mtendere: Dikira/ khala tcheru (5:1-12)

5:1	5:2-6	5:7-12

   b. Makhalidwe a mtendere: Tumikiranani wina ndi mnzake (5:13-15)
   c. Mphamvu ya Mtendere: Yendani ndi Mzimu (5:16-26)

5:16-24	5:25-26

   d. Kachitidwe mu mtendere: Chitani zabwino kwa anthu onse (6:1-10)

6:1-5	6:6-10

   e. Mathero (6:11-18)

Aefeso

(Khristu: Chuma Chathu mwa Mulungu kwa ife)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Monga m'mene zikuonetsedwera mu ndime zoyambirira za bukhuli komanso ku makalata olembedwa ali ku ndende, Paulo mtumwi akuoneka kuti ndiye mlembi wa bukhuli. Ndipo chilembedwe cha mutu wa bukhuli ndicho "kwa Aefeso".

Zaka: A.D. 60–61: Paulo anali kundende (Aefeso 3:1; 4:1; 6:20) pamene amalemba bukhu limeneli. Ophunzira akumasiyana pakuti kodi Paulo analemba kalatayi ali kundende ku Kaesareya (Machitidwe 24:27) mu AD. 57–59, kapena ali ku Roma (28:30) mu A.D. 60–62. Koma umboni waukulu umakamba za ku Roma. Mabukhu a Aefeso, Akolose, Afilipi ndi Filimoni analebedwa munthawi yofanana (Afilipi 1:7; Akolose 4:10; Filimoni 9). Chifukwa Aefeso sanatchule chifukwa chomwe Paulo anatulukira kundende, monga mu Afilipi (1:19-26) ndi Filimoni (1:22), izi zikuonetsa kuti bukhu ili la Aefeso linalembedwa masiku oyambirira a undende wa Paulo ku Roma mu A.D. 60, pamene anali mu ndende ya mnyumba ndi kulonderedwa ndi mlonda (Machitidwe 28:30). Paulo atatulutsidwa, analemba 1 Timoteo ndi Tito, ndipo anamangidwanso nalemba 2 Timoteo ndipo anaphedwa ku Roma komweko.

Mutu ndi Cholinga: Paulo akuonetsa kuti "Mpingo ndi thupi la Khristu," ndipo Khristu ndiye mutu wa Eklessia (1:22, 23) ndipo okhulupilira ndiwo okwira naye ntchito Yesu (1:3; 2:11-22). Paulo akulongosola izi mu njira ziwiri: akulongosola za chuma cha mdalitso wa okhulupilira Khristu, cha padziko ndi kumwamba (1:3-12).

Poyera, cholinga cha Paulo chinali chofuna kuchurukitsa malire a okhulupilira pa nkhani ya madalitso ndi chuma mwa khristu yemwe ali mutu wa mpingo, thupi la Khristu. Pambali pa zonsezi, zolinga ziwiri ziuluzikulu mu makalatawa zinali izi choyamba, kulongosola za madalitso ndi chuma chomwe Khristu amapereka kwa okhulupilira, ndi momwe kudzera mwa okulupilirawo, cholinga chosatha cha mulungu chinafikira kudzera mwa umunthu wa Khristu, pa zinthu za dziko ndi za kumwamba (1:3-12). Zoyenera kuchita anthu okhulupilira, mayendedwe, makhalidwe, mayankhulidwe, molingana ndi ufumu wa kuwamba (1:18-23; 3:14-21; 4:1).

Ngakhale sizinalembedwe pokonza zolakwika, Paulo anaumba kalatayi monga chiletso chotchingira anthu ku mavuto omwe amapezeka chifukwa chosakhwima ndi kulephera kugwiritsa ntchito Khristu,mu moyo wawo okhulupilirawo, ndipo amayanjana nsi Satana mmalo mwake (6:10-18). Chonco Paulo amalemba za chuma cha okhulupilira, mayendedwe ndi zisamaliro (6:10-18). Akupitilira kulongosola za mphoto ya kukhulupilira Mulungu.

Khristu mu Bukhuli: "Mawu oti'monga Khristu" kapena "Ndi Khristu" alembedwa mu bukhuli ka 35, ndipo ngakhale mawuwa Paulo anawakamba mu makalata ake ambiri, mu bukhu ili la Aefenso, wawalankhula mobwereza-bwereza kambiri kuposa ena onse. Mwa Khristu (1:1), kudalitsidwa ndi Khristu (1:3), kusankhidwa ndi iye (1:4), kutengedwa ndi Khristu (1:5), mokondedwa (1:6), owomboledwa mwa iye (1:7), olandira cholowa mwa iye (1:11), khala ndi chikhulupiliro ku ulemelero wa Khristu (1:12), omangiririka ndi mzimu kudzera mu cholowa (1:13-14), opangidwa amoyo, okhala ndi iye mmwamba (2:5-6), olengedwa mwa Khristu mu ntchito zabwinos (2:10), olandira malonjezano mwa Khristu (3:6) okhala ndi mwayi wa kwa Mulungu mwa chikhulupiliro kudzera mwa Khristu (3:12).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Malonje (1:1-2)**

2. **Gawo la Chiphunzitso cha Kalata: Kuitanidwa kwa Mpingo (1:3–3:21)**
   a. Mayamiko chifukwa cha Chiombolo (1:3-14)
   b. Pemphero la nzeru ndi Bvumbulutso (1:15-23)
   c. Chipulumutso chochokera mu chisomo (2:1-22)
      2:1-10 2:11-22
   d. Chinsinsi cha maitanidwe a amitundu (3:1-13)
   e. Paulo apempherera Aefenso (3:14-21)
      3:14-19 3:20-21

3. **Gawo Lina la Kalata: Makhalidwe a Mpingo (4:1–6:24)**
   a. Umodzi wa iwo a chikhulupiliro (4:1-16)
      4:1-6 4:7-16
   b. Mayendedwe olungama a wokhulupilira (4:17–5:21)
      4:17-24 5:1-2 5:6-14
      4:25-32 5:3-5 5:15-21
   c. Akhale akutsanza a Mulungu (5:22–6:9)
      5:22-24 6:1-8
      5:25-33 6:9
   d. Makhalidwe a okhulupilira pokhala ndi anzawo (6:10-20)
      6:10-17 6:18-20
   e. Mathero (6:21-24)

Afilipi

(Khristu: Kukwanira mu Zonse kwa Mulungu pa Ife)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Paulo ndiye mlembi wa bukhuli. Iyi inali kalata yomwe analembera ku mpingo wa ku Afilipi, mpingo woyamba womwe Paulo anakhazikitsa ku Makedonia, ndipo umatchedwa "mpingo wa ku Afilipi."

Zaka: A.D. 60–61 Monga ndi Aefenso, kalata iyinso inalembedwa pamene Paulo anali mndende. Umboni wake kwa mlonda wa ku Praetoria (Afilipi 1:13) ndi kutheka kwa imfa (1:20-26) zikusonyeza kuti kalatayi analemba ku Roma. Ngakhale chilango cha imfa chinali choyenera pa mlandu wake, iye anali ndi chikhulupiliro kuti atulutsidwa. Pali chitsimikizo chokwanira kuti bukhuli linalembedwa mu A.D. 60 kapena 61 atatha kulemba kalata yaku Aefeso.

Mutu ndi Cholinga: Monga Aefeso anakhazikitsa ulemerero wachinsinsiwu, "mpingo womwe ndi thupi la Khristu," ndipo Khristu kukhala mutu wa Eklesia (1:22-23) ndi okhulupilira kukhala m'bale ndi m'longo olandira dalitso limodzi mwa Khristu (1:3; 2:11-22), alonda a ku afilipi amatsutsana ndi chiphunzitso cha Chikhristu (Afilipi 1:27; 2:2; 4:1f.). Mutu wa bukhuli ndi "chimwemwe ndi umodzi mwa Khristu."

Zifukwa zomwe Paulo analembera kalatayi ndi izi: (1) Amafuna kusonyeza chikondi chake ndi chiyamiko chake pa mphatso yomwe inapatsidwa kwa iye (1:5; 4:10-19); (2) kuperekalipoti pa zomwe zinamuchitikira (1:12-26; 4:10-19); (3) kulimbikitsa afilipi kuti akhale olimba mchikhulupiliro pakati pa chitsutso (1:27-30; 4:4); (4) kuwalimbikitsa kuti akhale mu umodzi ndi kudzichepetsa (2:1-11; 4:2-5); (5) ku chitira umboni Timoteo ndi Epafrodito ku mpingo wa ku Afilipi (2:19-30); ndi (6) kuwachenjeza Afilipi pa zomwe amachita anthu a mudzikolo zophwanya malamulo, ndi zakuthupi (ch. 3).

Khristu mu Bukhuli: Za umunthu ndi umulungu wa Khristu zikupezeka pa (2:5-8). Mu zonse, Khristu anali, ali, ndipo wachita ndipo adzachita ndikumalizitsa zonse. Paulo akutchula Khristu monga: (1) moyo (1:21); (2) chitsanzo cha kudzichepetsa, ndi nsembe yachikondi (2:4-5); (3) yemwe adzasinthe matupi mu ulemelero wake pa chiukitso (3:21) ndi (4) wopereka mphamvu kwa ife mu nyengo zonse za pa moyo (4:12).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule[79]

1. **Malonje ndi Chithokozo pa Afilipi (1:1-11)**
   1:1-2 1:3-11

2. **Paul Aphunzitsa za Khristu (1:12-30)**

1:12-18	1:21-26	
1:19-20	1:27-30	

3. **Makhalidwe a Mkhristu (2:1-30)**

2:1-4	2:12-13	2:19-30
2:5-11	2:14-18	

4. **Mphoto pa Moyo wa Chikhristu: Chidziwitso mwa Khristu (3:1-21)**

3:1	3:7-11	3:17-21
3:2-6	3:12-16	

5. **Mtendere mu Moyo wa Chikhristu: Kudziwa kupezeka kwa Khristu (4:1-23)**

4:1-3	4:8-9	4:15-20
4:4-7	4:10-14	4:21-23

Akolose

(Khristu: Chidzalo cha Mulungu pa Ife)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Bukhuli mlembi wake ndi Paulo yemwe akupereka malonje pa 1:2, Kalatayi inadziwika kwa "Akolose."

Zaka: A.D. 60–61 Makalata aundende a Paulo omwe analemba koyamba ku Roma mu A.D. 60-61 (onani Aefenso ndi Afilipi).

Mutu ndi Cholinga: Cholinga ndi mphamvu yobala zipatso za uthenga wabwino womwe ufalitsa ukulu wake, utsogoleri wake, ndi chizalo chake chonse cha Khristu ku mpingo womwe ndi thupilake. Mu kalatayi, tikuona Paulo monga chithunzi cha Khristu.[80] Akolose akusonyeza kuti Yesu Khristu ndi Mulungu yemwe akukwaniritsa ntchito yake. Yesu chida cha okhulupilira, ndiye yankho lathu, pakuti iyeyu ndi wokwanira mu zones (2:10). Akolose akulongosola ukulu, kukwanira ndi kusafanana ndi munthu, kwa Yesu yemwe ndi mpulumutsi, mlengi, mthandizi ndi chosowa chirichonse pa munthu panyengo ino ngakhalenso nthawi za moyo wamuyaya.

Khristu mu Bukhuli: Wilkinson ndi Boa anati:

> Bukhu limodzi ili, lomwe lalongosola za Khristu, maziko ake ndi Khristu "mutu wa maukulu ndi mphamvu zonse" (2:10), mbuye wa chilengedwe (1:16-17), mwini wa kubwezeretsa (1:20-22; 2:13-15). Maziko a chikhulupiliro (1:5, 23, 27), maziko a mphamvu ya moyo watsopano kwa okhulupilira (1:11, 29), mpulimutsi ndi wokhululukira anthu okhulupilira (1:14, 20-22; 2:11-15), wodzala ndi chiyero (1:15, 19; 2:9) mlengi ndi mthandiziwa zones (1:16-17), mutu wa mpingo (1:18), Mulungu-munthu wodzukanso kwakufa (1:18; 3:1), mpulumutsi wosasowa kanthu (1:28; 2:3, 20; 3:1-4).[81]

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule[82]

1. **Chiphunzitso: Umunthu ndi Ntchito ya Khristu (1:1–2:5)**

1:1-2	1:13-14	1:24-29
1:3-8	1:15-20	2:1-5
1:9-12	1:21-23	

2. **Dongosolo: Asatsate Ziphunzitso Zonyenga (2:6–3:4)**

2:6-7	2:16-19	3:1-4
2:8-15	2:20-23	

3. **Ntchito: Ntchito Zabwino za Wokhulupilira Khristu (3:5–4:6)**

3:5-11	3:22-25	4:5-6
3:12-17	4:1	
3:18-21	4:2-4	

4. **Awachenjeza za Kupemphera ndi Kikhala nayo Nzeru (4:7-18)**

4:7-9	4:10-17	4:18

1 Atesalonika

(Khristu: Malonjezo a Mulungu kwa Anthu)

Mutu ndi Mlembi wa Bukhuli: Molingana ndi 1:1 ndi 2:18, Paulo ndiye mlembi wa bukhuli.

Zaka: A.D. 51–52 Makalata awiri a ku Atesalonika analembedwa ndi Paulo ali ku Akorinto mu miyezi 18 yomwe anakhalako (Machitidwe 8:1-11). Kalata yoyamba yaku Atesalonika inalembedwa Timoteo atangobwera kumene kuchokera ku Atesalonika ndi uthenga wa momwe wayenderako. Kalata yachiwiri inatumizidwa patatha milungu yochepanso. Izi zinali zaka za a A.D. 51-52.

Mutu ndi Cholinga: Paulo anakhala ku Atesalonika milungu itatu yokha (Machitidwe 17:2), choncho kunali kovuta kuti awaphunzitse zonse. Choncho cholinga cholembera kalatayi chinali chofuna kulongosola: kuthokoza pa zomwe Mulungu akuwachitira Atesalonika (1:2-3); kudziteteza yekha pa utumiki (2:1-12); kuwalimbikitsa kuti aime nji potsutsana ndi chitsutso chirichonse (3:2-3; 4:1-12); kuyankha mafunso onse a chiphunzitso cha Chikhristu, pokhuzananso ndi omwe anafa (4:1-13); kuyankha za "tsiku la Ambuye" (5:1-11); kuthana ndi mavuto omwe amapezeka ku mpingo (5:12-13; 19-20).

Khristu mu Bukhuli: Popeza mu chaputala chirichonse amakambamo za kubweranso kwa Ambuye, Khristu mu bukhuli akuonetsedwa ngati chipulumutso ndi chiyenmbekezo cha okhulupilira ntawi ino ngakhalenso irikudza. Akadzabwera Khristu, adzaombola tonse mu mkwiyo ndi muchisautso (1:10; 5:4-11), azatipatsa mphoto (2:19), kutiyeretsa (3:13), kutidzutsa kwakufa (4:13-18) kutiika pa malo abwino, a anthu okhulupilira (5:23).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Zipatso za Uthenga Wabwino ku Atesalonika (1:1–3:13)**

1:1-5	2:9-12	3:1-5
1:6-10	2:13-16	3:6-10
2:1-8	2:17-20	3:11-13

2. **Kupilira mu Chikondi (4:1-12)**

4:1-8	4:9-12

3. **Khama, Chikondano ndi Kuyeramtima (4:13–5:28)**

4:13-18	5:12-13	5:23-24
5:1-11	5:14-22	5:25-28

2 Atesalonika

(Khristu: Mphotho ya Mulungu pa Ife)

Mlembi ndi Dzina la Bukhuli: Mlembi ndi Paulo (2 Thessalonians 1:1; 3:17).

Zaka: A.D. 51–52 Bukhuli linalembedwa patangotha miyezi yosapyola isanu ndi umodzi chilembere 1 Atesalonika (1:4-5), malinga ndi zifukwa zina zomwe mlembi anaziona mu A.D. 51 kapena 52, atachoka Sila ndi Timoteo, Paulo anabwera ndi nkhani iyi yatsopano.

Mutu ndi Cholinga: Paulo amayankha malinga ndi zomwe anamva: (1) za kuchuruka kwa chisautso pa okhulupilira (1:4-5); (2) lipoti la makalata ena abodza okhuza "tsiku la Ambuye" (2:1f.); ndi (3) tmomwe ena amayankha pa za kubweranso kwa Ambuye. Choncho Paulo analemba kuti athetse bodza, ulesi ndi kusalongosoka kwa zinthu komwe kunakula mu mpingo (3:5-15).

Choncho Paulo analemba pofuna kutonthoza ndi kukonza zolakwika, iye analemba kuti: (1) awalimbikitse atesalonika kupilira powauza kuti kuli mphoto yaikulu ukatha moyo uno (1:3-10); (2) kulongosola bwino za tsiku la ambyuye (2:1-2); ndi (3) kupereka malangizo omwe mpingo ungatsate kuti uchite ntchito yoyenera ndi kutsutsana nacho choipa (3:6-15).

Khristu mu Bukhuli: Mutu weniweni wa kalatayi makamaka mu 1-2, ndi kubweranso kwa Khristu pa chiweruzo pomwe adzaike adani onse pansi kuchilango chosatha, ndi okhulupilira iye ku moyo wosatha. Bukhuli likutchula Khristu monga woweruza yemwe alinkudza.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Malonje (1:1-2)**

2. **Atesalonika Alimbikitsidwa nkana Atasautsidwa (1:3-12)**

3. **Asanabwere Khristu Adzaoneka okana Khristu (2:1-17)**
   2:1-12 2:13-15 2:16-17

4. **Machenjezo ndi Malankhulano (3:1-15)**
   3:1-5 3:6-13 3:14-15

5. **Malawilano, Moni ndi Mdalitso (3:16-18)**

1 Timoteo

(Khristu: Mkhalapakati Wathu kwa Mulungu)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Kalatayi analemba ndi Paulo Mtumwi kulembera kwa Timoteo. Timoteo anali mtumiki wang'ono ku Aefeso yemwe anakumana ndi zipsinjo mukutumikira kwake ku mpingowu. Paulo, monga mphunzitsi wa Timoteo, analemba makalata awiri kwa iye pofuna kumulangiza. Pa chifukwa ichi, Paulo analemba kwa Tito ku Krete.

Zaka: A.D. 63 Zikuoneka kuti pofanizira machitidwe a atumwi posiyanitsa ndi makalata, monga 1 Timoteo ndi Tito analembedwa pa nthawi youmwe Paulo anatulutsidwa mndende ku Roma. Pa chifukwa cha ichi, 1 Timoteo zikusonyeza kuti bukhu la 1 Timoteo linalembedwa mchaka cha A.D. 63, isanafike nthawi yake yosautsidwa ndi Nero mu A.D. 64. Bukhu la Tito linalembedwa mu chaka cha A.D. 65 ndipo 2 Timoteo inalembedwa mu A.D. 66. Paulo anamwalira mu A.D. 67, molingana ndi kholo la mbiri ya mipingo, Eusebius. Monga nzika ya chiRoma, Iye anamwaira ndi mkondo osati kupachikidwa monga anachitira Petro.

Maulendo a Paulo anachitika mu zaka za A.D. 48-56. Kuchokera mu A.D. 56-60 Paulo anayendetsedwa mu mabwalo a chiweruzo ambiri, mpaka ku Roma. Kwa zaka ziwiri, A.D. 61-62, Paulo anaikidwa mu nyumba ya ndende, ndipo anaturutsidwa. Kuchokera A.D. 62-67 Paulo anayenda momasuka, kumusiya Timoteo mu Aefenso ndi Tito mu Krete, ndipo anakwanitsa kuwaembera makalata. Choncho 1 Timoteo ndi Tito analembedwa mu A.D. 63-65. Atagwidwanso Atagwidwa ndi kumangidwanso, Paulo analemba kwa Timoteo, kalata wachiwiri, 2 Timoteo mu A.D. 66, yomwe inali kalata yotsiriza ya Paulo.[83]

Mutu ndi Cholinga: Zifukwa zisanu zomwe analembera kalatayi ndi izi: (1) kulimbikitsa ndi kukulitsa uzimu ndi kulimba mtima kwa Timoteo pomukumbutsa kuti atumikire Mulungu moyenerera (1:3), za mphatso yake ya uzimu (4:14), za chivomerezo chake (6:12) ndi kukhazikika kwa chiphunzitso chomwe chinaikidwa mwa iye (6:20); (2) kumupatsa Timoteo mayankho a mu Baibulo okhudzana ndi aneneri onyenga ndi kumulimbikitsa kuti apitilize kukhala pa chiphunzitso choyenera (1:3-11, 18-20; 4:1-16; 6:3-10); (3) Kulongosola dongosolo la zochitika mu mpingo ndi popembeza (2:1-15); (4) kulongosola za zoyenera akulu a mpingo ndi Atumiki (madikoni) (3:1-16) ndi mkhalidwa weniweni wabwino (5:1-20); ndi (5) kuwachenjeza kuti atsutsane ndi zoipa ndi ziphunzitso zonyenga (6:11-19).

Mutu wa mu 1 Timoteo, monga ndi Tito ndi 2 Timoteo, akulongosola za munthu ndi mpingo. Kwa munthu, mutu wake ndi ***"kulimbana nako kulimbana kwabwino"*** (1:18). Ku mpingo, mutu wake ndi, kayendetsedwe ka mpingo, nyumba ya Mulungu (3:15).

Khristu mu Bukhuli: Ndime zambiri zaima pa mfundo ya utumiki ndi mpilimutsi. Yesu Khristu ndiye maziko a maitanidwe athu, mphamvu zathu, chikhulupiliro ndi chikondi chomwe chikufunika mu utumiki (1:12-14); Yemwe anabwera kupulumutsa ochimwa (1:15); ***"mkhala pakati wa anthu ndi Mulungu"*** (2:5); ***"Mulungu wozionetsera yekha kuthupi, wopanda chimo, woonedwa ndi angelo, wolalikidwa kwa amitundu, wokhulupiliridwa padziko lonse, wolandira ulemelero"*** (3:16); ndi ***"mpulumutsi kwa anthu onse, makamaka kwa okhulupilira"*** (4:10).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Malonje (1:1-2)**

2. **Malangizo pa Ziphunzitso (1:3-20)**
   1:3-7 1:12-17
   1:8-11 1:18-20

3. **Malangizo pa Mapempheredwe (2:1-15)**
   2:1-7 2:8 2:9-15

4. **Malangizo pa Atsogoleri (3:1-16)**
   3:1-7 3:8-13 3:14-16

5. **Malangizo pa Zoopsa, Mmasiku Wotsiriza (4:1-16)**
   4:1-5 4:6-10 4:11-16

6. **Malangizo Okhudzana Maudindo (5:1–6:10)**
   5:1-2 5:17-22 6:1-2
   5:3-8 5:23 6:3-10
   5:9-16 5:24-25

7. **Malangizo Otsirizo kwa Timoteo (6:11-21)**
   6:11-16 6:17-19 6:20-21

2 Timoteo

(Khristu: Woweruza)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Wonani ku 1 Timoteo

Zaka: A.D. 66 Onani 1 Timoteo

Mutu ndi Cholinga: Tikalowa mu 2 Timoteo tiona kuti talowa ndime yovuta kwambiri. Mu 1 Timoteo, ndi Tito, Tikuona kuti Paulo anali ndi ufulu woyenda, koma mu 2 Timoteo, Paulo anali mdende, mpaka chilango chophedwa. Mu kalatayi, Paulo anlemba ndi zolinga ziwiri: (1) Kumuitana Timoteo kuti apite ku Roma mwachangu iye asanafe (cf. 4:9, 21 ndi 4:6-8); ndi (2) Kulimbikitsa Timoteo kuti amangilirike mu chiphunzitso chenicheni cha Chikhristu, kuti adzikwanitsa kuziteteza pa zoopsa ndi kupilira monga msilikali wabwino, pozindikira kuti tiri mu nyengo yowawitsa.

Monga 1 Timoteo, pali mgwirizano weniweni pa mutu wa bukhuli Kwa munthu; mutu wake ndi ***"ukoleze mphamvu ya Mulungu, iri mwa iwe mwa kuika manja anga"*** (2 Timoteo 1:6), ngakhale pali mavesi ambiri omwe angapange mutu wa bukhuli, paokha kapena mogwirizana ndi ena (1:14; 2:1-2; 2:15; 4:5). Ku mpingo, mutu wake ndi kubweretsa chiphunzitso chokhazikika kwa athu okhulupilika a Mulungu, kuti iwonso, athe kuphunzitsa ena mu chisautso ndi mazunzo a msilikali wokhulupilika wa Khristu (2:2-4), kapena kulimbana nako kulimbana kwabwino ndikutsiriza njirayo (4:6-7).

Khristu mu Bukhuli: Pachimake penipeni pa bukhuli,pali utumiki wakupilira mu chiphunzitso cha Ambuye Yesu Khristu. Ndi zosadabwitsa, choncho kuti ngakhale mu bukhuli akutsindika za chipiliro monga maziko a chiphunzitsochi. Mu bukhuli akulongosoledwa ngati, yemwe ***"anatha imfa, naonetsera poyera moyo ndi chisabvundi, kudzera mu uthenga wabwino"*** (1:10), monga yemwe anauka kwakufa (2:8), yemwe amapereka chipulumutso ndi ulemerero wamuyaya (2:10), yemwe okhulupilira amwalira mwa iye, naukitsidwanso mwa iyes, ndi kudzera mwa iye tilandira mphoto ya kukhulupilika monga korona wachipulumutso ndi mpata wokhalanso mu ulamuliro wake (2:11-13; 4:8).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Malonje (1:1-2)**

2. **Ayamika Mulungu Chifukwa cha Timoteo (1:3-7)**

3. **Apemphedwa Akumbukire Ntchito ndi Udindo Wake (1:8-18)**
   1:8-14 1:15-18

4. **Khalidwe Loyenera Mtumiki wa Mulungu (2:1-26)**
   2:1-7 2:14-19
   2:8-13 2:20-26

5. **Zoipa Zoopsa, Mmasiku Otsiriza (3:1-17)**
   3:1-9 3:10-17

6. **Awalamulira Alalikire Mawu a Mulungu (4:1-5)**

7. **Chitonthozo kwa Mtumiki wa Mulungu (4:6-18)**
   4:6-8 4:9-15 4:16-18

8. **Mathero, Moni ndi Mdalitso (4:19-22)**

Tito

(Khristu: Kukoma Mtima kwa Mulungu pa Anthu)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Makalata a ubusa anenedwa kale ndi alembic ake, (onani 1 Timoteo).

Tito sanachulidwepo mu Machitidwe a atumwi, koma walongosoledwa kwambiri mu makalata a Paulo (ka 13). Izi zikutsimikizira kuti Tito anali wokwira naye ntchito wa Paulo, wokhulupilika pa uthenga wabwino. Pamene Paulo anachoka ku Antiokeya kupita ku Yerusalemu kukakambirana thenga wa chisomo (Machitidwe 15:1f.) ndi atsogoleri kumemeko, anatenganso Tito (wa mitundu) (Agalatiya 2:1-3) monga chitsanzo cha munthu wovomerezedwa mwa chisomo, osati mwa mdulidwe (Galatians 2:3-5). Zikuonekanso kuti Tito anagwira ntchito ndi Paulo Mtumwiyo ku Aefeso mu ulendo wake wachitatu. Kuchokera kumeneko, Paulo anamtuma Tito ku Akorinto komwe anathandiza pa ntchito ya mpingo (2 Akorinto 2:12-13; 7:5-6; 8:6).

Zaka: A.D. 65 Zolembedwa za mu kalatayi zingathe kupereka nthawi yomwe bukhuli linalembedwa, ngakhale nthawi yeniyeni siikudziwika. Paulo anatulutsidwa mu nyumba ya ndende ku Roma (komwe tikuona kutha kwa Machitidwe a Atumwi). Paulo anali mzika ya chiRoma ndipo anthu omutsutawo analephera kupereka mlandu weniweni wa iye, ndipo anasankha kuti asakamuweruze kwa Kaisara (Machitidwe 24-25; 28:30). Omutsutsawo, anagonja pa mulanduwo ndipo Paulo anaturutsidwa. Mtumwi anapita ku Aefenso, komwe anasiya Timoteo kuti aziyang'anira mpingo ndipo anapitiliranso ku Makedonia (kumpoto kwa dziko la Greece), ndipo analemba 1 Timoteo (1 Timoteo 1:3). Ndipo anapitanso ku Krete, namusiya Tito kuti alongosole zina ndi zina za ku mpingo wa ku Krete. Atachoka apo, Paulo anapita ku Nikopoli mu Achaia (kumpoto kwa Greece, Tito 3:12). Ndipo anapita ku Macedonia kapena Nicopolis, Paulo ndipo, analemba kalata kwa Tito yomulangiza ndi kumulimbikitsa. Atatha apo, anapitanso ku Troa (2 Timoteo 4:13) komwe anamangidwa, natengeredwa ku Roma, naikidwa mundende, namuphas. Monga takamba kale, kunali Ku Roma, pa undende wake wachiwiri pomwe analemba 2 Timoteo. Izi zinachitika mu A.D. 62–67.

Mutu ndi Cholinga: Pali mitu ndi zolinga zosiyanasiyana za kalatayi. Paulo analemba: (1) kumulangiza Tito za zomwe angachite kuti akonze zolakwika ndi zosoweka mu dongosolo la kukhazikitsa mipingo ku Krete; (2) kupereka kwa Tito chivomerezo ndi chilimbikitso mmavuto omwe amakumana nawo (2:15; 3:1-15); (3) kupereka malangizo a momwe angachitire pothana ndi chisutso. Komanso malangizo apadera okhuza chikhulupiliro ndi makhalidwe abwino; (4) anamuchenjezanso za aphunzitsi onyenga (1:5, 10-11; 2:1-8, 15; 3:1-11); ndi (5) kuonetsera malingaliro ake okumana naye Tito ku Nicopolis mu nyengo ya chisanu (3:12). Sitikudziwa ngati kukumanaku kunachitikadi kapena ayi, koma mbiri imati Tito anabwerera ku Krete komwe anakhala moyo wake wonse.

Mutu wa bukhuli ndi kufuna kuonetsa momwe chisomo cha Mulungu chomwe chinaokera kwa ife kudzera mu imfa ya Khristu, ndipo akutilangiza za kukana zamdziko ndi kukhala wolungama monga okhulupilira a Mulungu Mutu wa bukhuli ndi kufuna kuonetsa momwe chisomo cha Mulungu chomwe chinaokera kwa ife kudzera mu imfa ya Khristu, ndipo akutilangiza za kukana zamdziko ndi kukhala wolungama monga okhulupilira (2:10–3:9).

Nkhani zambiri zofunika zalembedwamo mu kalatayi kuphatikizapo zoyenereza akulu a mpingo (1:5-9), malangizo kwa anthu a zaka zosiyanasiyana (2:1-8), ubale ndi atsogoleri ndi olamulira (3:1-2), pogwirizana ndi ntchito zabwino ndi za Mzimu (3:5) ndi ntchito ya chisomo pa kukulitsa ntchito zabwino pamaso pa ana a Mulungu (2:11–3:8).

Khristu mu Bukhuli: Mothandizana ndi ziphunzitso za Paulo, tikuona momwe akhristu amakhalira pa moyo wathupi ndi uzimu, kale, lero ndi mtsogolo. Mu bukhu ili tikuona Umulungu (2:13) ndi ntchito yoombola ya Mpulumutsir (2:12). Apa Yesu akufotokozedwa monga ***"Mulungu ndi Mpulumutsi wathu, Yesu Khristu, yemwe anapereka moyowake kwa ife kutiombola ku ntchito zoipa, ndi kudziyeretsera anthu a iye mwini, wachangu ndi wantchito zabwino"*** (2:13-14).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Malonje (1:1-4)**

2. **Zoyenera Oyang'anira (Akulu a Mpingo) (1:5-9)**

3. **Obweretsa Chipsinjo pa Mpingo (1:10-16)**

4. **Dongosola la Zochitika mu Mpingo (2:1–3:11)**

2:1-2	2:9-10	3:1-11
2:3-5	2:11-14	
2:6-8	2:15	

5. **Malangizo Omaliza, Moni, ndi Mdalitso (3:12-15)**

Filemoni

(Khristu: Chikhulupiliro cha Mulungu pa Ife)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Monga mabukhu amakalata ena a undende (Aefeso, Afilipo ndi Akolose), bukhu la Filemon linalembedwa ndi Paulo mu nthawi yomwe iye anali mu mbindikiro ku Roma. Kalatayi inalembedwa kwa Filimoni, mwini wa Onesimo, mmodzi ma akapolo zikwi zikwi mu ufumu wa Roma. Onesimo adaba kwa Filimoni ndikuthawa. Onesimo mukubwerera kwake anakunana ndi Paulo ku Roma yemwe anamutumikira ndikumulozetsa ku Chikhristu (1:10). Apa tsono zinaoneka kuti Filimoni ndi Onesimo onsewa akala anthu a Chikhristu, ndipo Onesimo anayenera kubwereranso kwa Filimoni kuti akamupepese ndi kulandira chikhululukiro monga mbale mwa Ambuye. Malinga ndi malamulo akale, kapolo akathawa, napezekanso, anayenera kuphedwa, koma mu kalatayi, Paulo akudandaulira Filimoni, mmalo mwa Onesimo, kuti achitiridwe chifundo.

Zaka: A.D. 60–61 Pozindikira kuti bukhuli linalembedwa Paulo ali mu ndende koyamba ku Roma, kalatayi inalembedwa mu zaka za A.D. 60–61.

Mutu ndi Cholinga: Cholinga cha kalatayi chinali chopempha Filimoni kuti amukhululukire Onesimo ndikumubwezera ntchito yomwe amagwira, monga mbale osatinso monga kapolo (1:10-17). Paulo akupempha Filimoni kuti mangawa onse a Onesimo, awawerengere pa Paulo kuti alipire. Ndipo bukhuli likuonetsera Khristu yemwe analolera kumva zowawa chifukwa cha ife (1:18). Cholinga chachiwiri chinali chophunzitsa moyo wa Chikhristu mu machitidwe athu pa moyo wathu wa tsiku ndi tsiku. Zikusinthanso maubale omwe analipo pakati pa anthu (kapolo, wantchito, mkaidi). Mu mabukhu ena a undende, Paulo anayankhulanso za ubale watsopanowu (Aefenso 6:5-9; Akolose 3:22; 4:1). Mu kalatayi tiri ndi chitsanzo chogwirika pa nkhaniyi. Cholinga chotsiriza cha Paulo chinali chofuna kuonetsa kuthokoza kwa Filimoni pomupatsa iye zakudya pamene anali mdende (1:4-7, 22). Mutu weni weni ndi mphamvu ya uthenga wabwino imasintha moyo ndi nyengo zamunthu kuchoka pa chipsinjo kufika pa mtendere, ku ukapolo kufika pa ubale.

Filimoni sanali yekhayo kapolo mu mpingo wa ku kolose (Akolose 4:1), choncho kalatayi ikupereka ndonomeke ya momwe mabwana ena a Chikhristu amakhalira ndi akapolo awo. Paulo samaphwanya ufulu pomuuza Filimoni za Onesimo, koma amafuna kumukumbutsa ndi kumupempha kuti achite naye Filimoni monga Mabwana ena a Chikhristu achitira ndi akapolo awo (1:16). Komanso Paulo ananena kuti anali okonzeka kulipira zomwe Onesimo adaba kwa Filimoni. Pamatsiriziro, zikuoneka kuti Filimoni anakhululukira Onesimo namutumizanso kwa Paulo, ndipo mabukhu ena amati, Onesimo anakhala mtumiki wa Mulungu mpaka udindo wa Bishop ku mpingo wa ku Aefenso (1:14).[84]

Khristu mu Bukhuli: Chikhululukiro chomwe okhulupilira amachilandira kwa Khristu akalapa, ndi chomwe chikuoneka pa Filimoni ndi Onesimo yemwe analakwa kwambiri (1:11, 18), koma Paulo atapemphera mmalo mwake, zinasinthika (1:10-17). Paulo kupatulapo udindo wake (1:8) ndi chifukwa cha Onesimo, analolera kupempherera Onesimo kuti mangawa ake akhululukidwe (1:19). Mwa ntchito za chifundo ndi chisomo kwa Filemoni, Onesimo anaikidwa pa ubale, kuchoka pa ukapolo (1:15-16). Muzochitika izi ifenso tiri ngati Onesimo. Pemphero la Paulo kwa Filimoni ndichimodzimodzinso Yesu Khristu yemwe akupembezera monga nkhalapakati, wotiimilira kwa Atate. Onesimo anali wolakwa pa chilamulo koma anapulumuka mwa chisomo.[85]

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Pemphero la Chiyamiko kwa Filimoni (1:1-7)**
   1:1-3 1:4-7

2. **Pempho la Paulo Lokhudza Onesimo (1:8-18)**
   1:8-9 1:10-16 1:17-18

3. **Lonjezo la Paulo kwa Filemono (1:19-21)**

4. **Nkhani Zina (1:22-25)**

Gawo 3
Makalata Ena

Malonje: Pano tikambirana za makalata asanu ndi atatu a mu Chipangano Chatsopano, ndipo asanu ndi awiri a iwo, ndi otchedwa Makalata ena, kapena Makalata a mipingo yonse ngakhale analembedwa mu chi hebri. Makalatawa ndi osiyana ndi a Paulo aja chifukwa a Paulo anali olembera ku mipingo kapena kwa munthu.[86] Ndipo malembedwe awo, makalata enawa (kupatulapo 2 ndi 3 Yohane), sankalemberedwa dera limodzi ayi. Ndipo tikuona kuti Yakobo ndi bukhu lomwe likulemberedwa kwa ***"Mapfuko khumi ndi iwiri ya Israeli yomwe imakhala maiko akunja,"*** okhulupilira Mulungu kulikonse (monga Ayuda onse pa nthawiyo). Ndipo 1 Petro akulemberedwa omwe si nnzika koma afalikira ku "Pontiyo, Galatiya, Kappadocia, Asiya and Bituneya." Makalata a 2 ndi 3 Yohane akukhudzanso gulu ngakhale kuti alembedwera anthu owerengeka okha. Chifukwa cha kusiyanaku, mu maphunziro ano a akutchedwa dzina loti "makalata ena." Choncho, tiyenera kudziwa kuti makalata a Paulo sankaleberedwa potchula munthu, koma kuti kupatulapo Ahebri, mabukhu a makalata ena onsewa malinga ndi maina a alembi ake.

Mwachidule, Yakobo ndi Petro woyamba akulongosola za zoipa ndi zabwino, powadandaulira okhulupilira kuti ayende mayendedwe a Khristu Yesu. Petro wachiwiri, ndi Yuda ndi mabukhu a uneneri, ochenjeza okhulupilira kuti asamakhulupilire aneneri onyenga. Bukhu la Ahebri ndi makalata wa a Yohane akulongosola za Khristu, kuitanira akhrist kuti akhale mwa Yesu monga vumbulutso lomariza la Mulungu ndi chikwaniritso cha lonjezano chipangano chakale, ndikuti anthuwa asatayike koma akhalebe mu choonadi cha Mulungu kudzera mu uthenga wake wabwino.

Makalata asanu ndi atatuwa akutenga gawo lomodzi mwa magawo khumi a chipangano chatsopano ndipo akuonjezera pa mabukhu khumi ndi atatu a Paulo aja pogwirizana mu nkhani zina ndi zina za kukula mu choonadi. Aliyense mwa alembiwa (Yakobo, Petro, Yohane, Yuda ndi mlembi wa Ahebri) anathandiza kwambiri poumba moyo wa Chikhristu pa okhulupilira. Monga mmene makalata a Paulo alili, vumbulutso la chipangano chatsopano, akatha machitidwe a atumwi sikukanakhala bwino ngati mabukhu enawa a makalata sanakalembedwanso.[87]

Ahebri
(Khristu Yesu: Dzina Loposa Maina Onse)

Mlembi ndi Dzina la Bukhuli: Kwa zaka 1,200 (A.D. 400–1600) bukhuli limatchedwa, "Kalata wa Paulo Mtumwi kwa Ahebri," koma mu zaka zoyambirira panalibe chitsimikizo chenicheni cha dzina mlembi wa bukhuli.

Anthu akamba zambiri za bukhuli koma zoona zake ndi zoti mlembi, nthawi ndi malo olembera bukhuli sakudziwika.

Koma ngakhale zinali choncho pa (13:18-24). Akunena kuti, panali maganizo ogawikana pa mingo woyamba za mlembi wa bukhuli. Ena amati Paulo ndipo ena amatchula Barnaba, Luka kapena Clement, enanso amati sakudziwika mlembi. Koma kuzama ndi makulidwe a uzimu, zikuchitira umboni kuti mawu a mu bukhu la Ahebri ndi ouziridwa ndi Mulungu, posasamala kuti mlembi sakudziwika.

Popeza olandira kalatayi sanachulidwe mu Makalata a Paulo ,tingathe kunena mawu pa makalatawa.molingana ndi ndemanga za mabukhu ena a mu chipangano chakale mu makalatawakomanso kutsindika kwa nsembe mlembi wina wotchedwa: Zane C. Hodges ananena kuti bukhuli limalembedwera Ahebri; ndipo analongosola motere:

> Sakudziwika kwenikweni awerengi a bukhuli, komabe molingana ndi zolembedwamo (10:32-34); mlembi ankadziwa nkhani zawo zakale ndi zatsopano zomwe (6:10); ndipo anakwanitsa kukamba mwa chindunji (5:11-14). Choncho zikuoneka kuti mlembi anali pa ubale wabwino ndipo ankawadziwa bwino awerengiwa, mpaka ankanena zokawachezera, mwina pamodzi ndi Timoteyo (13:19, 23). Mlembi anawapemphanso kuti azimupempherera (13:18).
>
> Mopanda chikaiko chirichonse, mlembiyo anali wachiyuda makhalidwe ake, ngakhale nthawi zina, enanso akutsutsa izi. Inde ankalembera Ahebri. Inde anakambanso za amitundu, koma amatsindika pakuwadzudzula kuti sakutsata malamulo komanso choonadi. Ndipo iye amawadandaulira kwakukuru kuti kuti awalemekeze ndi kumvera mawu omwe iwo anakula nawo, a mu bukhu lopatulika,makamaka a mu chipangano chatsopano osati chakale.[88]

Zaka: A.D. 64–68 Mabukhu ambiri akuti Ahebri analembedwa mu A.D. 64-68. Clement wa ku Roma, anayankhulaponso za bukhuli mu A.D. 95. Choncho zikutitsimikizira kuti bukhuli linalembedwa ntawiyi isanafike. Komaso zikuoneka kuti bukhuli linalembedwa Yerusalemu asanaonongeke (mu A.D. 70) pa zifukwa izi: (1) mlembi akadalembamo za kuonongeka kwa Kachisi ndi kutha kwa nsembe zopsereza za chi Yuda; (2) mlembi walongosola za Kachisi ndi oyenera kuchita mu Kachisi ndi popemhera, izi zikusonyeza kuti bukhuli linalembedwa Kachisi asanaonongedwe (5:1-3; 7:23, 27; 8:3-5; 9:6-9, 13, 25; 10:1, 3-4, 8, 11; 13:10-11); (3) mlembi akulongosolanso za kumaslidwa kwa Timoteyo 13:23, polumikiza ndi ulendo womwe anayenda ndi Paulo ku Roma cha mu ma A.D. 60.

Mutu ndi Cholinga: Mutu wa bukhuli ndi ukulu ndi ulemelero woposa zones, wa Khristu. Mawu oti "bwino, opanda banga, ndi zakumwamba" akulongosoledwa mu bukhuli poikira umboni pa izi. Mlembi akutionetsera mfundo zisanu zosonyeza kuti Khristu ndi woposa ndi wabwino: (1) Ku aneneri a chipangano chakale (1:1-3); (2) angelo (1:4–2:18); (3) Mose (3:1-6); (4) Yoswa (3:7–4:16); (5) Unsembe wa Aaroni (5:1–10:18). Cholinga cha mutu uwu chinali kufuna kuchenjeza anthu kuopsa kwa kupereka ungwiro wawu wa Chikhristu, kwa zithunzi za mchipangano chakale (10:1). Kuti owerenga akhwime mu chikhulupiliro ndi kukwaniritsa maitanidwe awo. Choncho, mlembi analemba machenjezo asanu, motere (2:1-4; 3:1–4:13; 5:11–6:20; 10:26-39; 12:14-29).

Khristu mu Bukhu: Pokwaniritsa cholinga chofuna kuonetsera za ukulu wa Khristu, bukhu la Ahebri lakhala limodzi mwa mabukhu omwe alongosola bwino za Khristu ndi chiphunzitso chake, mu chipangano chatsopano. Khristu akulongosoledwa monga Mwana, pofuna kuonetsera kuti iye amaimilira Mulungu Atate (1:3, 13), monga wokhala pa dzanja lamanja la Mulungu (1:3), yemwe anatchula Mulungu Atate, kuti ndiye Mulungu yekhayo (1:8-9), mlengi wa nthawi zamuyaya (1:10-12) wansembe wanthawi zamuyaya, malinga ndi mdondomeko ya Melikizedeki (ch. 7). Mu bukhuli, Khristu akuonetsedwa monga mneneri wolungama, wansembe, komanso mfumu. Iye ndi momboli, yemwe analolela kukhala mbale, nathana ndi tchimo, nazipereka yekha nsembe pantanda paja, nakwera kumwamba atauka mmanda, ndipo anakhala wansembe wamkulu wosenza zofooka ndi mavuto athu.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Khristu Mwana wa Mulungu Aposa Onse (1:1–7:28)**
   a. Khristu aposa Aneneri a m'chipangano chakale (1:1-3)
   b. Khristu aposa Angelo (1:4–2:18)
      1:4-14 | 2:5-8 | 2:14-18
      2:1-4 | 2:9-13
   c. Khristu aposa Mose (3:1-6)
   d. Khristu aposa Yoswa (3:7–4:13)
      3:7-11 | 4:1-5
      3:12-19 | 4:6-13
   e. Khristu aposa Unsembe wa Aaroni (4:14–7:28)
      1) Kugwiritsitsa choonadi (4:14-16)
      2) Zoyenera Wansembe (5:1-10)
         5:1-4 | 5:5-10
      3) Asakhale a ulesi mu uzimu (5:11–6:12)
         5:11-14 | 6:1-8 | 6:9-12
      4) Malonjezano a Mulungu salephereka (6:13-20)
      5) Yesu Khristu, Mkulu wa nsembe (7:1-28)
         7:1-3 | 7:11-22
         7:4-10 | 7:23-28

2. **Yesu Khristu ndiye Nkhoswe ya Chipangano Chosatha (8:1–10:39)**
   a. Pangano Latsopano (8:1-13)
      8:1-6 | 8:7-13
   b. Chihema chatsopano (9:1-10)
      9:1-5 | 9:6-10
   c. Nsembe yatsopano (9:11–10:18)
      9:11-14 | 9:23-28 | 10:11-18
      9:15-22 | 10:1-10
   d. Chilimbikitso (10:19-39)
      10:19-25 | 10:26-31 | 10:32-39

3. **Chikhulupiliro (11:1–12:29)**
   a. Zitsanzo za anthu a Chikhulupiliro munthawi yakale (11:1-40)

11:1-2	11:13-16	11:30-31
11:3-7	11:17-22	11:32-38
11:8-12	11:23-29	11:39-40

   b. Kupilira mwachikhulupiliro (12:1-11)

12:1-2	12:3-11

   c. Awalimbikitsa akhalebe mchikhulupiliro (12:12-17)

12:12-13	12:14-17

   d. Zotsatira pa akukhulupilira (12:18-29)

12:18-24	12:25-29

4. **Mathero (13:1-25)**
   a. Moyo wakuchita mawu, makhalidwe a Khristu (13:1-17)

13:1-6	13:7-14	13:15-17

   b. Apempha okhulipilira kuti amupempherere (13:18-19)
   c. Madalitso/ pemphero la mdalitso (13:20-21)
   d. Zolankhula zina (13:22-23)
   e. Kupereka moni ndi Kutseka kalata (13:24-25)

Yakobo

(Khristu: Chitsanzo Chathu)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Kalata iyi yayamba ndi mawu oti ***"Yakobo, kapolo wa Mulungu ndi Ambuye Yesu Khristu, kwa mafuko khumi ndi awiri a mchibalaliko"*** (1:1). Mu mu chipangano chatsopano anayi omwe atchulidwa ndi dzina la Yakobo, ndipo ndi awa: (1) Mwana wa zebedayo (Marko 1:19); (2) mwana wa alefeyo (Marko 3:18); (3) Tate wa Yudasi (osati Isikarioti) (Luka 6:16); ndi (4) mbale wa Ambuye Yesu (Agalatiya 1:19). Ndipo Ryrie analemba motere za Yahobo:

> Mwa anthu anayi omwe maina awo anali Yakobo mu chipangano chatsopano, ndi anthu awiri okha omwe anaganiziridwa kuti analemba bukhu la Yakobo–Yakobo mwana wa Zebedayo (mbale wa Yohane) ndi Yakobo, mbale wake wa Yesu. Komabe, palibe chitsimikizo kuti mwana wa Zebedayo anali mlembi wa bukhuli, pozindikira kuti iyeyu adaphedwa mu A.D. 44 (Machitidwe 12:2). Malinga ndi malembedwewa, (Yakobo wang'ono ndi Yakobo wa ku Luka 6:16) siomwe analemba bukhuli ayi, koma Yakobo mbale wa Yesu yemwe anakhala wodziwika mu mpingo waku Yerusalemu (Machitidwe 12:17; 15:13; 21:18). Izi zikutsimikizikanso pofananiza mawu a Yakobo mu chigiriki pa msonkhano wa ku Yerusalemu (Yakobo 1:1 ndi Machitidwe 15:23; Yakobo 1:27 ndi Machitidwe 15:14; Yakobo 2:5 ndi Machitidwe 15:13).[89]

Molingana ndi momwe Yakobo akuyankhulira, anthu olandira uthengawu ayenera adziwidwe ndi kulongosoledwa. Yakobo amalembera ***"kwa mafuko khumi ndi awiri omwe anamwazikana kunja kwa dziko lawolawo"*** (1:1). Monga anena kuti "Abale anga" mu 1:19 ndi 2:1, 7, uwu ndi umboni kuti kumwazikana uku sikuja kwa mu A.D. 66-70, koma kumwazikana kwa akhristu achiyuda kuchoka mu dziko lawochifukwa cha zovuta zina (Matthew 1:11, 12, 17). Mu mabukhu oyambirira a machitidwe, Ayuda ankakhala ku Yerusalemu kuchokera ku maiko onse pa phwando la Pentekosite (Machitidwe 1:5). Ambiri mwa iwo anaona zozizwz pa Pentekosite ndipo anayamba kukhulupilira Khristu. Ndipo, patapita nthawi, iwo anabwerera mu maiko ndi madera a kwawo. Awa ndi womwe Yakobo ankawalembera kalata iyi.

Zaka: A.D. 45 kapena **46** Bukhu la yakobo, inali kalata yoyamba kulembedwa ndipo munali mu zaka za A.D. 45. Zifukwa zake ndi izi: (1) Pali nkhani zambiri zomwe zalembedwamo zachiyuda kutsimikizira kut mu nthawiyi anthu adali asanachoke mu chikhalidwe cha chiyuda. (2) Bukhuli silinakambepo zotsutsana ku Mdulidwe wa chiyuda. (3) Mawu oti Sunagogi amlembedwamo kutanthauza malo osankhika okumanirako, kapena kuti tchalitchi (2:2). (4) Kusowa kwa mfundo yokhudzana ndi oweruza mlandu a ku Yerusalemu pofanizir a akhristi achiyuda ndi akhristu amitundu (Machitidwe 15:1f., A.D. 49). (5) "Kuchitira umboni kwa ziphunzitso za Yesu kukusonyeza kuti kalatayi inabwera zitatha izi."[90]

Mutu ndi Cholinga: Yakobo amakhuzidwa ndi kukhala ndi chikhulupiliro chenicheni ndi chofunika, champhamvu, chotakataka, ndi cha ntchito zake. Yakobo akulemba kuwachenjeza okhulupilira za zotsatira za akufa, a chikhulupiliro chopanda pake, ndikuwaunikira mu njira.

Khristu mu Bukhu: Ya kukula ndi kuzama mu uzimu. Mu 1:1 ndi 2:1, Yakobo akulongosola chindunji za "Ambuye Yesu Khristu" ndi kuongosola za kubweranso kwake kwa chiwiri (5:7-8). Mu mavesi 108 a kalatayi,

mukupezeka maumboni ochokera mu mabukhu 22 a mchipangano chatsopano ndi pafupifupi ziphunzitso 15 za Yesu pa chiphunzitso cha Paphiri.[91]

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule[92]

1. **Kuima pa Chikhulupiliro (1:1-27)**
   a. Malonje (1:1)
   b. Chimwemwe mu nthawi ya mayesero (1:2-12)
      1:2-4 1:5-8 1:9-12
   c. Kumkana Mdiyerekezi (1:13-18)
   d. Tikhale akuchita Mawu (1:19-27)
      1:19-25 1:26-27

2. **Kutumikira ndi Chifundo (2:1-26)**
   a. Asachite Tsankhu pakati pa anthu (2:1-13)
      2:1-7 2:8-13
   b. Kuthandiza osowa (2:14-26)
      2:14-17 2:18-26

3. **Azichenjera ndi Pakamwa Pawo (3:1-18)**
   a. Zoyankhula (3:1-12)
      3:1-5 3:6-12
   b. Nzeru yochokera kumwamba (3:13-18)

4. **Kulapa (4:1-17)**
   a. Kuchotsa kuzikudza, kukhala anthu odzichepetsa (4:1-6)
   b. Kuweruza (4:7-12)
      4:7-10 4:11-12
   c. Lekani kunyada, khalani ndi chikhulupiliro mwa Mulungu (4:13-17)

5. **Kugawirana (5:1-20)**
   a. Kugawirana zinthu (5:1-6)
   b. Kupilira ndi kuleza mtima (5:7-12)
   c. Kupemphererana (5:13-20)
      5:13-18 5:19-20

1 Petro

(Khristu: Chitsanzo Chathu mu Nthawi ya Msautso)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Ndime yoyambirira ikunena kuti Mtumwi Petro ndiye Mlembi wa Bukhuli (1:1). Bukhuli linavomerezedwa monga ntchito ya Petro Mtumwi ku mpingo woyambirira.

Kalatayi imalemberedwa anthu aku Pontio, Galatia, Kappadocia, Asiyaa ndi Bituneya omwe anali okhulupilra osankhidwa (1:1). Awa anali okhulupilira a chiYuda ndi amitundu omwe omwe anakhala mu maiko a padziko lapansi. Mau oti "Omwazikana" matanthauza AYuda okhala ku Palestina ndikufalikira mu dziko lonse lozungulira Nyanja ya Medeterenian. Apa akukambanso za akhristu amitundu omwe amakhala mu maiko a anthu osapembeza Mulungu wamoyo.[93] Petro ankalingalira ayuda ndi amitundu okhulupilira.

Kalata yoyamba ya Petro ikulemberedwa Akhristu omwazikana mu zigawo zonse zisanu za ulamuliro wa chiroma ndi m'Asiya komwe lero ndi ku mpoto kwa dziko la Turkey. Mipingo ya madera awa inali ya aYuda ndi amitundu. Kalatayi inali yodzadza ndi maumboni a zolembedwa za mu Chipangano Chakale. Akhristu achiYuda anatchulidwa kuti Otchona (DIASPORA) potanthauza kuti omwazikana mmene mlembi amalemba malonje pa (1:1). Awa ndi ayuda omwe amakhala kunja kwa mzinda wa Yerusalemu.

Amitundu anawerenga momwe Petro anakwezera kuunika kolungama, pa mawu a Mulungu (1:14). Amitundu anakondweranso podziwa kuti anali mu nthawi yakusadziwa yomwe Mulungu anawalekelera, kom atsono ndi anthu owerengeredwa, ana a Mulungu. Petro anayankhula ndi onse ayuda ndi amitundu omwe mu kalata yake yachikimbikitsoyi, ku mipingo yaku Asiya.[94]

Zaka: A.D. 63–64 Mbiri ya mpingo imalongosola kuti izi zinachitika mu zaka zomaliza za utumiki wa mtumwi Petro ku Mzinda wa Roma. Molingana ndi nkhani yak u Baibulo pa 5:13, umboni wotsindikizidwa ku Roma, kalatayi inalembedwadi mmene Paulo anali ku Roma zaka za A.D. 63, usanafike mliri wa kuphedwa kwa Nero

mu A.D. 64. Petro sanatchulepo Roma ngati mdani wa Chikhristu (1 Petro 2:13-17). Izi zikusonyezadi kuti bukhuli linalembedwa muliri wa Nero usanachitike.

Mutu ndi Cholinga: 1 Petro akulongosola ziphunzitso zosiyana siyana zokhudza moyo wa Chikhristu. Mutu ndi cholinga cha 1 Petro unali pa kuzunzika kudzera mu chisautso cha anthu okhulupilira. Bukhuli latchulidwanso kuti bukhu landondomeko zophunzitsira pa moyo wa Chikhristu, mmene ali padziko kwakanthawi kochepa, podikira Ufumu wa Yesu Khristu (1:1, 13-21; 2:11-12; 3:14, 17; 4:1, 13, 15, 16, 19).

Bukhuli likulongosola mfundo zitatu motere: (1) kuunikira kubweranso kwa Khristu ndi chiombolo chake (1:3-12); (2) kutsatira Khristu pakulandira ndi kumva zowawa (2:21-24); ndi (3) pa kukhala mu dziko molingana ndi maitanidwe monga osankhidwa a Mulungu ndi kukhala pfungo labwino ku dziko (2:4-12; 4:1-19). Zolinga zina zinali kufuna kuonetsa mgwirizano pakati pa chiphunzitso ndi ntchito zabwino (5:12) ndi kulimbikitsa atsogoleri a umulungu kuti awetebe nkhosa za Mulungu (5:1-4), zomwe ndi zothandiza kuti mpingo ukule ndi kukhala wochitachita muuzimu, ntchito ndi choonadi.

Khristu mu Bukhuli: Bukhuli ladzadza ndi nkhani za munthu ndi ntchito za Khristu. Kudzera mu kuuka kwake kwa Khristu, Akhristu ali ndi chiyembekezo chokhalanso ndi moyo, moyo opanda chibvundi (1:3-4). Petro akulongosola za ulemelero ulinkudzawo ndi bvumbulutso la Khristu (1:7, 13; 4:13; 5:1). Akukambanso za umunthu ya Yesu Khristu, monga Mwanawankhosa wa Mulungu, yemwe anatiombolo posenza matchimo athu pantanda (1:18-19; 2:24). Komanso kuti Khristu ndi chitsanzo chathu chopanda chenicheni cha mazunzo (2:21-24) ndi Mbusa wathu wamkulu yemwenso ndi mtetezi wa okhulupilira (2:25; 5:4).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Chipulumutso kwa Okhulupilira (1:1-12)**
   a. Malonje (1:1-2)
   b. Tsogolo (la oyera mtima) Chiyembekezo ndi Mayesero mu nyengo inu (1:3-9)
   c. Chipulumutso nthawi ino ndi Bvumbulutso la kale (1:10-12)

2. **Kuyeretsedwa kwa Okhulupilira (1:13–2:12)**
   a. Awadandaulira atsate kuyeramtima (1:13-21)
      1:13-16 1:17-21
   b. Awadandaulira akhale okondana (1:22-25)
   c. Mkaka woyenera wa mawu opanda chinyengo (2:1-3)
   d. Awadandaulira akhale akupereka nsembe zauzimu (2:4-10)
      2:4-8 2:9-10
   e. Awadandaulira azikanize ku zilakolako za thupi (2:11-12)

3. **Okhulupilira Azigonjera (2:13–3:12)**
   a. Azigonja ku mafumu ndi atsogoleri (2:13-17)
   b. Azigonja pakuchita zabwino (2:18-20)
   c. Atenge chitsanzo cha Khristu (2:21-25)
   d. Kugonjerana mu banja (akazi ndi amuna) (3:1-8)
   e. Kulolera masautso monga anachita Ambuye (3:9-12)

4. **Kumva Zowawa (3:13–5:14)**
   a. Makhalidwe oyenera pamene mumva zowawa (3:13-17)
   b. Khristu chitsanzo cha kumva zowawa ndi kuzigonjetsa (3:18–4:6)
      3:18-22 4:1-6
   c. Machenjezo pa kumva zowawa (4:7-19)
      4:7-11 4:12-19
   d. Zoyenera akulu ndi anyamata, adzichepetse, adikira (5:1-11)
      5:1-5 5:6-11
   e. Mathero / Malawilano/ Mdalitso (5:12-14)

2 Petro

(Khristu: Mawu Enieni)

Mlembi ndi Dzina la Bukhu: Mlembi wa bukhuli ndi Simon Petro (1:1). Pali zitsimikizo zambiri kuti mlembi wa bukhuli ndi Petro Mtumwi. Mu malembedwe ake, pafupifupi pa chipangano chotsiriza cha Atate Wotiferayo, mlembi amagwiritsa ntchito dzina loti “Iye” (1:14) pofuna kutsimikizira kuti iye analidi mboni yeniyeni, yemwe anaona Yesu akuwalitsidwa paphiri paja (1:16-18 cf. Mateyu 17:1-5). Ndipo malembedwe a bukhu lino akusonyeza kuti bukhuli linali lachiwiri kulembedwa ndi mlembiyu (3:1), ndipo amasonyezanso kuti anakhalapo

ndi Paulo Mtumwiyo, yemwe amamutchula “Mbale wanga wokondedwa” (3:15). Mukhuli lotchedwa “Kalata wachiwiri wa Petro Mtumwi,” pofuna kusiyanitsa ndi kalata yoyamba ya Petro.

Petro amalembera kalatazi ku mtundu umodzi wa okhulupilira (3:1) monga kalata yake yoyamba. Ndi pangano lomariza, chenjezo lomaliza ndi “kalata ya tsiku lomariza” (1:14; 2:1-22; 3:3). Ankalembera kalatayi kwa akhritu a chikhulupiliro chofanana, mosakaikisa; amalembera ayuda ndi mipingo ya amitundu yaku “Pontiyo, Galatiya, Kappadocia, Asiya, and Bituneya” (1 Petro 1:1).

Zaka: A.D. 67–68 Monga kalata ya malawirano, Petro analemba kalatayi kumapeto kwa ntchito yake (1:12-14). Malinga ndi wolemba mbiri wina wotchedwa, Eusebius, Petro anaphedwa ndi mfumu Nero (pafupifupi A.D. 67-68). Kalatayi inalembedwa mu zaka zimenezi.

Mutu ndi Cholinga: Monga Mtumwi Paulo anachenjeza za choopsa chomwe chikubwera mu masiku otsiriza, mu mapeto a utumiki wake (2 Timoteo), choncho, Petro anachenjezanso za choopsacho cha aneneri onyenga, monga zinaneneredwa ndi Aneneri, ndi Ambuye Yesu Khristu mwini, komanso ndo Atumwi ake (2:1; 3:1-3). Cholinga chenicheni cha kalata yaifupiyi, ndi kuchenjeza za choopsa chomwe mpingo ukumane nawo, makamaka, za aphunzitsi onyenga.

Poona kuti Mulungu anapereka zonse zofunikira mu moyo (1:3), 2 Petro ndi bukhu lomvera anthu chifundo ndikuwapempha kuti akule ndi kukhwima mwa Khristu, Asakhale aulesi, asakhalenso osabereka zipatso (1:8) ndipo ndi maziko awa, akhale tcheru pozindikira aneneri onyenga. Izi zinatero chifukwa Petro amadziwa kuti masiku ake okhala moyo padziko lapansi, ndi owerengeka (1:13-15) ndi kuti thupi la Khristu linakumana ndi zoopsamu nthawiyo (2:1-3). Choncho, Petro analakalaka kukumbutsa anthu mu malingaliro awo (1:13; 3:1-2) kuti adzale ndi chiphunzitsochi mumalingaliro awo (1:15). Pochita izi, anawalongosola okhulupilira okhwima muuzimu, kuwalimbikitsa kuti akule mu zisomo ndi chidziwitso cha Mpulumutso (1:2-11; 3:18).

Monga chiphunzitso cha mmene angadziwire aneneri onyenga, Petro analongosola za mawu a Mulungu monga maziko oona (1:12-21) ndipo anachenjeza za zoopsa ndi aneneri onyenga omwe anawatchula chiweruzo choona (2:1-22). Potsiriza, iye analimbikitsa awerengi ndi kutsindika kwa kubweranso kwa Khristu (3:1-16). Ndipo Petro akulongosola kotsiriza kuti:

> ***Inu tsono, okondedwa, pozindikiratu izi, chenjerani, kuti potengedwa ndi kulakwa kwa iwo osayeruzika, mungagwe kusiya chikhazikiko chanu. Koma kulani muchisomo ndi chizindikiritso cha Ambye wathu ndi Mpulumutsi Yesu Khristu, kwa iye kukhale ulemerero, tsopano ndi nthawi zones. Amen*** (2 Petro 3:17-18).

Khristu mu Bukhuli: Petro akulongosola Khristu monga chiyambi cha Moyo ndi Mulungu, ndi kuyang’anisitsa. Mlembiyu akunena kuti Khristu ndiye “Ambuye ndi Mpulumutsi,” Iye wanenapo izi kanayi konse, ndipo wamutchula Yesu kuti “Iye” kwa ka khumi ndi mphambu zinayi. Poonjezera apa, iye anakumbusanso za “Mawalitsidwe a Yesu paphiri aja” ndikuti tiri kudikira kudza kwake kwa chiwiri kwa Mpulumutsi. Mu nthawi yakubweranso imeneyi dziko lonse lidzaona zomwe Petro ndi ophunzira ena awiri aja anaziona paphiri paja ali ndi Yesu.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Malonje (1:1-2)**

2. **Chiwombolo ndi Kulongosola za Khalidwe la Chikhristu (1:3-21)**
   a. Kukula kwa chikhulupiliro (1:3-11)
      1:3-4 1:5-8 1:9-11
   b. Makhalidwe a chikhulupiliro (1:12-21)
      1:12-15 1:16-18 1:19-21

3. **Aphunzitsi Onyenga (2:1-22)**
   a. Kuopsa kwa khalidweli (2:1-3)
   b. Chiweruzo ndi chionongeko (2:4-9)
   c. Makhalidwe ndi maonekedwe a aphunzitsi onyenga (2:10-22)

4. **Chikhulupiliro Chawo ndi Tsogolo (3:1-18)**
   a. Aphunzitsi onyenga (3:1-7)
      3:1-2 3:3-7
   b. Kuchedwa kwa tsiku la Ambuye (3:8-9)
   c. Zochitika potsatira Tsiku la Ambuye (3:10-13)
   d. Zofunikira mu nthawi ya zoopsa (3:14-18)

1 Yohane

(Khristu: Kukhutitsidwa ndi Mawu a Mulungu)

Mutu ndi Mlembi la Bukhuli: Ngakhale mlembi wa bukhuli sakupezeka mu bukhuli, dzina la mlembiyu silikupezekanso mukalatayi, Komabe chitsimikizo chiripo kuti Mtumwi Yohane ndiye mlembi wa bukhuli. Mlembiyu anali mmodzi wa mboni zenizeni za Mpulumutsi, Yesu Khristu, yemwe anamudziwa ndi kumuona maso ndi maso (1:1-5).

Mu bukhu lonseli, muli ma vesi omwe amanena kuti Yohane anali kulembera kalatayo anthu okhulupilira (2:1, 12-14, 19; 3:1; 5:13), komabe, mlembiyu sakulongosola kuti amalembera makalatayi kwa ndani, ndipo amakhala kuti? Pa chifukwa ichi, tingathe kuganizira kuti kalatayi amalembera ku mipingo yosiyanasiyana. Mwina inali mipingo yaku Aefenso.

Kalata woyamba wa Yohane anagwiritsidwa ntchito kwambiri ku Asiya (Turkey), komwe nthawiyo kunali mzinda wa Aefenso. Clement waku Alexandria (mbusa wa mzaka 100 zoyambirira) analongosola kuti Yohane anakhalako ndi kutumikira mu mipingo yosiyanasiyana mu mzindawu. Ndipo zikuoneka kuti bukhu la 1 Yohane linalembedwa ndi kutumizidwa ku Asiya.[95]

Zaka: A.D. 85–90 Ndi kovuta kutchula tsiku lenileni la 1 Yohane komanso mabukhu a makakata onse a Yohane, koma chifukwa mitu yake sikusiyana kwenikweni ndi uthenga wabwino wa yohane; zaoneka kuti analemba chisanafike chisautso cha Domitian in A.D. 95. Choncho, zaka zake ziyenera kukhala A.D. 85-90.

Mutu ndi Cholinga: Mutu wabukhuli ndi chiyanjano ndi Mulungu kudzera mwa Ambuye, Yesu Khristu (1:3-7). Makamaka potsutsana ndi chiphunzitso chomwe chinaliko mu nthawiyo (amakhulupilira kuti chikhulupiliro pa zinthu ndi choipa ndipo kuti ufulu umapezedwa kuchokera ku chidziwitso basi), Yohane analemba bukhuli pofuna kulongosola khalidwe wa chiyanjano ndi Mulungu yemwe (yohane) amamutchula kuti Kuwala, chikondi ndi moyo. MMulungu ndi kuwunika (1:5), Mulungu ndi chikondi (4:8, 16) ndipo Mulungu ndi Moyo (1:1-2; 5:11-13). Kuyenda mu chiyanjano ndi Mulungu, kukutanthauza kuti kuyenda mu kuwunika komwe kumabweretsa moyo wake, chikondi chake pa anthu ena ndi pa anthu olungama. Bukhuli limatiuza mayeso osiyanasiyana ndi mfundo zotsimikizira chiyanjano, kuzera mu mayeso a chipulumutso. Koma pogwirizana ndi mutu wa bukhuli, ziphunzitso za aphunzitsi onyenga ndi makhalidwe ake monga okhulupilira, ndi zabwino kuti tione mayeso ndi zitsimikizo za chikhulupilirozi mokhudzana ndi kumdziwa Khristu mpulumutsiyo, ndi bale wosintha miyo yathu.

Izi zikuoneka mu nkhani ya bukhuli malinga ndi zomwe ohkulupilira amakumana nazon, zovuta kuzilongosola, koma mu 1 Yohane, akulongosola chikaniro cha zoonadi za umunthu wa Yesu Khristu chomwe chimachinga chiyanjano pakati pa munthu ndi Mulungu. Yohane analemba kuti “ana inu” (2:1, 18, 28; 3:7, 18; 5:21) pa zifukwa zisanu: (1) Kulimbikitsa chiyanjano choona (1:3f.); (2) kuti anthu aone chimwemwe chodzadza (1:4); (3) Kulumbikitsa chiyero kudzera mu chiyanjano choona (1:6-2:2); (4) Kutchnjiriza kuti anthu asachimwe (2:18-27); ndi (5) kupereka chitsimikizo (5:11-13).

Khristu mu Bukhuli: Bukhuli likuonetsetsa za utumiki wa nthawi ino wa Mpulumutsi ndi moyo wa okhulupilira amene amadikira kubweranso kwake. Mwazi wake ukupitilirabe kutiyeretsa ku uchimo (1:7) andipo kuchokera pa tchimo ndi kusalungama, kufikira mu kulapa kwa machimo (1:9). (2:1) Ndipo nsembeyi si ya kwa okhulupilira kale okha koma kudziko lonse lapansi (2:2); Zoonadi, ukulengeza kuti Khristu ndiye choonadi ndi wotinenera kwa Atate (2:1); ndikuti Yesu ndi Khristu yemwe analonjezedwa kuti adzakhala (2:22; 4:2-3); anabwera mu madzi ndi mwazi, umboni kudzera mu ubatizo ndi kufa pamtanda (5:6); ndi kubweranso kwake padziko kachiwiri, momwe tidzamuona maso ndi maso monga mmene alili (2:28–3:3).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Malonje ndi Cholinga cha Kalatayi (1:1-4)**

2. **Zoyenereza mu Chiyanjano (1:5–2:2)**
   a. Kuyenda Mu kuunika kwa Mulungu (1:5-7)
   b. Kulapa machismo ndi kukhululukidwa (1:8–2:2)
      1:8-10 2:1-2

3. **Makhalidwe Oyenera (2:3-27)**
   a. Makhalidwe abwino mu chiyanjano–Kukhala ngati Khristu (2:3-11)
      2:3-6 2:7-11

b. Malamulo a Chiyanjano–Kudzimana za padziko (2:12-17)
   2:12-14 2:15-17
c. Chenjezo kwa okhulupilira–Za okana Khristu (2:18-27)
   2:18-25 2:26-27

4. Anthu a mu Chiyanjano cha Khristu (2:28–5:3)
a. Chiyero (2:28–3:3)
   2:28-29 3:1-3
b. Chilngamo, pounikiranso infa ya Khristu (3:4-24)
   3:4-10 3:13-22
   3:11-12 3:23-24
c. Kuyesa Mizimu (4:1-6)
   4:1-3 4:4-6
d. Mulungu ndiye Chikondi, za kukonda Mulungu ndi kukondana ndi abale (4:7–5:3)
   4:7-14 4:15-21 5:1-3

5. Zotsatira za Kukhulupirira Yesu (5:4-21)
a. Chigonjetso cha okhulupilira (5:4-5)
b. Umboni wa Khristu (5:6-12)
c. Chitsimikizo cha chipulumutso cha okhulupilira (5:13)
d. Kuyankhidwa kwa pemphero (5:14-17)
e. Chigonjetso pa uchimo (5:18-21)

2 Yohane

(Khristu: Chikondi cha Mulungu)

Mlembi ndi Dzina la Bukhuli: Ngakhale sananene bwino za mlembi. Pali chitsimikizo kuti mlembi wa bukhuli ndi Yohane mtumwi. Iye amadzitcha "mkulu wa mpingo" pofuna kusunga popanda phokoso kuti analembanso mabukhu a uthenga wabwino wa Yohane, ndi 1 Yohane ndi 3 Yohane. Monga mkulu wa mpingo, zikusonyeza kuti kuti amagwiritsa bwino ntchito udindo wakewu, ndipo iye anali wodziwika bwino ku mbiri ya utumiki.

Bukhli latchulidwa "kalata wachiwiri wa Yohane."

Kalatayi imalemberedwa ***"kwa mkazi wosankhidwa ndi ana ake"*** (1:1, 4-5). Ndipo sakudziwika kuti amenewa anali yani.

Zaka: A.D. 85–90 Ndi kovuta kutchula tsiku lenuleni, koma malinga ndi zochitika zolembedwamo, pali umboni kuti analembedwa nthawi imodzi ndi 1 Yohane (A.D. 85–90).

Mutu ndi Cholinga: 2 Yohane, ndi kalata youza awerengi kuti ayende mu choonadi malinga ndi malamulo a Mulungu (1:4-6). Popeza ***"anthu onyenga ambiri afalikira pa dziko, anthu omwe savomereza Khristu yemwe anabwera mwa thupi"*** (1:7). Yohane amalemba poteteza anthu kuti asachite zoipa koma akhale mu choonadi pa zifukwa ziwiri izi: (1) amafuna kuti owerenga asaphonyane ndi mphoto ya moyo wosatha (1:9) ndi (2) kufuna kupereka malangizo omveka a za aneneri onyenga omwe ali mmakomo ndi mipingo. Yohane samafuna kuti anthu onyengawo aloledwe mmanyumba ndi mumipingo ndikutengedwa ngati aphunzitsi olondola, Iye amafuna kuchenjeza anthu kuti azisiyanitsa wonyenga ndi wolalikira uthenga weniweni.

Khristu mu Bukhuli: Monga mu 1 Yohane, 2 Yohane akukhuza za kuteteza chilungamo cha chiphunzitso cha mu Baibulo choti Yesu ndi Mulungu yemwe anbwera pa dziko monga munthu, ndipo onse otsutsana ndi izi, ndi onyenga.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Chiyambi ndi Malonje (1:1-3)**

2. **Umboni wa Kuyenda mu Choonadi (1:4)**

3. **Lamulo la Chikondano (1:5-6)**

4. **Machenjezo ndi Malangizo, Achenjere ndi Aphunzitsi Onyenga (1:7-11)**

5. **Mathero (1:12-13)**

3 Yohane
(Khristu: Dzinalo)

Mlembi ndi Dzina la Bukhuli: Mtumwi Yohane ndiye mlembi weniweni wa kalatayi. Mu 2 ndi 3 Yohane, mlembiyo akuzilingosola yekha monga "mkulu wa mpingo" ndipo mawu oterewa amapezeka mu makalata onse: "chikondi mu choonadi" (1:1) mu makalata onse awiriwandi "kuyenda mu choonadi" (1:4 ya makalata awiriwo).

Makalata a Yohane akulongosola motere, ndipo kalata iyi amalembere "Gayo, wokondedwa" (1:1) pa nkhani za mpingo ndi mavuto omwe Gayo amakumana nawo. Gayo anali wodziwika ku mipingo yak u Asiya komwe Yohane anatumikirako pa zaka zomariza za moyo wake. Gayo ndi dzina lodziwika bwino ku mabukhu a chipangano chatsopano. Dzinali likuoneka mu Aroma 16:23 (Gayo wa ku Korinto), Acts 19:29 (Gayo wa ku Makedonia) ndi Machitidwe 20:4 (Gayo wa ku Derbe), padalibe mgwirizano weniweni pa anthu awa ndi Yohane.

Zaka: A.D. 85–90 Ndipo, kufanana pakati pa 1 ndi 2 Yohane akulongosola kuti analembedwa zaka zofanana A.D. 85-90.

Mutu ndi Cholinga: Yohane akulembera Gayo malinga ndi kulandira bwino, kuthandiza ndi kusamalira kwake atumiki a Mulungu (missionaries), makamaka alendo. Apa zikupereka chitsimikizo cha kufanana pakati pa utumiki wa Gayo ndi ntchito zake zachifundo pa chikondi mu Chikhristu, monga woyenda mu choonadi, kwa makhalidwe lodzikonda a Diotrefe yemwe, mmalo moyenda mu choonadi, anakana zomwe Yohane ananena, ndipo Detrofe amafuna kungochemeleredwa (1:9).

Bukhuli liri ndi mfundo izi: (1) kulamula Gayo (1:1-6a); (2) kulangiza ndi kulimbikitsa chifukwa cha thandizo lake kwa atumiki a Mulungu omwe Yohane ankawatuma (1:6b-8); (3) kudzudzula Deotrofe chifukwa cha khalidwe lake lozikonda (1:9-11); (4) kupereka malangizo kwa Demetriyo (1:12); ndi (5) kudziwitsa Gayo za chikhumbo cha Yohane kukamuchezera ndiku thana nazo zovuta zonse (1:10a, 13-14).

Khristu mu Bukhuli: Ngakhale dzina la Yesu Khristu silinalembedwe mwachindunji, komabe akutchulidwa munkhaniyi motere: ***"Popeza apita chitsogolo ndi 'Dzinalo.'"*** Uwu ndi umboni ku utumiki, mmalo mwa Yesu Khristu (Machitidwa 5:40-41 pomwe mu chigiriki alongosola mu 5:41). Paulo akuyankhula monganso mu Aroma 1:5. Mu 1 Yohane, Yohane akuti: ***"Machimo anu akhululukidwa mu Dzina la Yesu Khristu."*** Uthenga wabwino wa Yohane ukuchitira umbonimu kukhulupilira ***"Mdzina la Yesu Khristu"*** (John 1:12; 3:18).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Malonje (1:1)**

2. **Umboni wa Gayo (1:2-8)**
   a. Kuopa Mulungu (1:2-4)
   b. Za kuchereza abale/ Ntchito za Chifundo (1:5-8)

3. **Za Diotrefe (1:9-11)**
   a. Maganizo ake opanda pake (1:9)
   b. Ntchito zake zamatama/zozikudza (1:10-11)

4. **Demetriyo (1:12)**

6. **Mawu Otsiriza (1:13-14)**

Yuda
(Khristu: Chitetezo pa Munthu)

Mlembi ndi Dzina la Bukhuli: Mlembi wa bukhuli ndi Yuda (1:1). Mu chiGiriki dzinali ndi Yudasi. Dzinali ku chingerezi anagosintha kuti Yuda kuti asiyanitse ndi Yudasi yemwe anamupereka Khristu. Mlembi wa bukhuli, akudziwikanso monga mbale weniweni wa Yesu, mng'ono wake. Yuda ali pa mdandanda ya abale a Yesu mu Mateyu 13:55 ndi Marko 6:3.

Ndi zothandiza kuti muzindikire izi:

> Ngakhale Yuda anali mbale wake wa Yesu, iye anali wodzichepetsa pamodzi ndi Yakobo, mbale wake winayo. Iye akudzitchula yekha Kapolo wa Yesu Khristu, ndipo zikusonyeza kuti samakhala onyada ngakhale mbale wake anali Yesu. Popeza Yuda linali dzina losasowa mwa anthu ambiri mu zaka za mma 100 AD (ophunzira awiri a Khristuomwe anali ndi dzina la Yuda,

kuphatikizapo yemwe anamupereka Yesu, choncho Yuda mlembiyu, amatchulidwa Yuda, mbale wa Khristu.[96]

Kalatayi amalembera kwa akhristu onse, osati pa munthu mmodzi ayi, kapena gulu limodzi la anthu ayikoma ***"kwa onse oyitanidwa, okutiridwa mu chikondi cha Mulungu, Atate ndi kusungidwa ndi Khristu Yesu"*** (1:1). Ndipo amawatchula iwo "okondedwa" kapena "abale okondedwa" (1:3).

Zaka: A.D. 70–80 Ngakhale zolembazi zikufananirako ndi 2 Petro. Kusiyana kwa Yuda ndi 2 Petro ndi koti Petro amachenjeza kuti "kuli aphunzitsi onyenga" (2 Petro 2:1), Yuda anati "kuli anthu ena omwe akugwa mwa chinsinsi pakati panu" (1:4). Choncho 2 Petro amakamba za vuto lomwe Yuda analikamba la zochitika za lero, Komatu Yuda anlemba bukhuli, Petro atalemba kale 2 Petro. Ngati 2 Petro analembedwa mu A.D. 67–68, ndiye Yuda analembedwa cha mu A.D. 70-80.

Mutu ndi Cholinga: Yuda amalongosola za chipulumutso, koma chifukwa cha zoopsa zomwe mipingo inkakumana nazo, iye amapempha mmalo molimbikitsa okhulupilira kuti ateteze chikhulupiliro chawo ndikuthana ndi aphunzitsi onyengaomwe amapezeka mu mipingo.[97]

Yuda analembedwa pa zifukwa izi: (1) kudzudzula khalidwe loipa lomwe anthu amachita, loipitsa ndi kudetsa mipingo ndi kubvunditsa okhulupilira, ndi (2) Kulangiza okhulupilira kuti akhale angwiro mu chikhulupiiliro, apitirize kukula mu chikhulupiliro pamene ali mu choonadi.

Khristu mu Bukhuli: Yuda akutiphunzitsa kuti tikhulupilire Yesu Khristu monga chitetezo chathu (1:24), pa moyo wamuyaya (1:20) ndi pa kubweranso kwake (1:21). Ndi Yesu yekha yemwe amatilumikizitsa ndi Mulungu (1:25).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Malonje (1:1-4)**

2. **Za Aphunzitsi Abodza (1:5-16)**
   a. Chiweruzo chakale (1:5-7)
   b. Chiweruzo cha nthawi ino (1:8-13)
   c. Chiweruzo cha nthawi ya mtsogolo (1:14-16)

3. **Chitetezo ndi Kukwezedwa kwa Okhulupilira (1:17-23)**

4. **Kulawirana / Mdalitso (1:24-25)**

Gawo 4
Bukhu La Uneneri

Chibvumbulutso
(Khristu: Wobweranso Padziko)

Malonje: Bukhu la Chibvumbulutso tikuona kuti likutsiriza za mavumbululutso a Mulungu kwa anthu. Monga Genesis liri bukhu la ziiyambi, Chibvumbulutso ndi bukhu lamathero. Bukhuli likulongosola za zochitika mu masiku otsiriza, ndi kubweranso kwa Ambuye, kulamuliranso kwa Ambuye, ndi moyo wosatha. Tikayang'ana, zochitika mu baibulo, pali mitu yambiri yomwe ikupezekamo monga: kumwamba ndi pansi, tchimo, themberero ndi chisoni, munthu ndi chipulumutso chake, satana, kugwa ndi chionongeko chake; Israel, kusankhidwa kwake, kudalitsidwa kwake, kulangidwa kwake, mafuko ake, Babulo ndi anthu ake, ndi maufumu. Ndipo nkhani zonsezi tizipeza zikukwaniritsidwa mu bukhu la Chibvumbulutso. Mabukhu a uthenga Wabwino ndi makalata anayamba ndi kumangilira zonsezi pamodzi, koma zonsezi zinakwaniritsidwa ku bukhu la chibvembulutso.

Tiyeni tione ndandanda uwu:

Bvumbulutso: Kukwaniritsidwa kwa Baibulo

Chipangano Chakale ndi Chatsopano	
Kumwamba ndi ku Chionongeko →	Bukhu la Chibvumbulutso
Munthu–chilengedwe, kuchimwa, chipulumutso →	
Tchimo–chiyambi, temberero, chisoni →	
Satana–khalidwe, kuchimwa, chilango →	
Mapfuko–kusamvera, zipembezo →	
Israeli–chisankho, madalitso, chilango →	
Mpulumutsi wolonjezedwa–ntchito, lamulo →	
Ufumu–malonjezo, pulogalamu →	

Mlembi ndi Dzina la Bukhuli: Momwe bukhuli lafotokozera, mlembi wake anali Yohane (1:4, 9; 22:8). Yohane anali mneneri (22:9) ndi mtsogoleri wodziwika bwino ku mipingo yaku Asiya komwe iye amalemba bukhuli la Chibvumbulutso (1:4).

Yohane ameneyu, ankadziwika kuti Yohane Mtumwi, mmodzi mwa ophunzira khumi ndi awiri a Yesu Khristu, Ambuye wathu. Malembedwe ake pa bukhuli ndi osiyana ndi mmene analembera uthenga wabwino wa Yohane, ndipo malembedwe awa, akutitsimikizira ulosi ndi uneneri wake.

Zaka: A.D. 96 Bukhuli Linalembedwa munthawi ya ulamuliro wa Domitian, ndipo popeza izi zatsimikizidwanso ndi alembic ena, monga Clement wa ku Alexander ndi Eusebius, ophunzira ambiri amakhulupilira kuti bukhuli linalembedwa pakati pa A.D. 81-96. Ndipo ili ndilo tsimikizo choti bukhuli ndi lotsiriza pa mabukhu a chipangano chatsopano, atangomaliza Uthenga wabwino ndi makalata ake atatu aja.

Mutu ndi Cholinga: Bukhu la Chibvumbulutso ukukhudzana ndi mkangano pakati pa munthu (motsogozedwa ndi Satana), ndi chigonjetso cha chimwemwe pogonjetsa adani ndi kukhazikitsa ufumu wa zaka chikwi (zaka 1,000 mu Chibvumbulutso 20).

Izi zikutsimikiziridwa kwa awerengi mu (1:3) polongosola zochita za Satana monga mizu ya zoipa mdziko lapansi. Bukhu la chivumbulutso likutionetsera mphamvu yogonjetsa yomwe iri mwa Mkango wa pfuko la Yuda (Yesu), mphukira wa Davide. Mkangowu, ukuonekanso monga mwana wa nkhosa woimilira, wophedwa, komanso wokhalabe ndi moyo, wokwiya komanso wobweretsa chiweruzo mu chiyero cha Mulungu, pogonjetsa tchimo ndi kugalukira kwa dziko lapansi.

Muli anthu osiyanasiyana mu bukhuli, ndipo alembedwa malinga ndi ntchito yomwe anagwira. Anthuwa ndi awa: Ambuye Yesu Khristu, Yohane Mlembiyo, ndi mboni ziwiri; chilombo choturuka munyanja, ndi Aneneri onyenga, ndipo potsiriza Mkwatibwi yemwe adzabwere ndi Ambuye Yesu.

Khristu mu Bukhuli: Popeza bukhu la Chibvumbulutso ndi bukhu la "mabvumbulutso/ maulosi a Yesu Khristu." Bukhuli limationetsera Ulemerero, nzeru ndi mphamvu (1:1-20) ndi ulamuliro Wake ku Mpingo (2:1–3:22). Ndi mpando wake wa Chiweruzo ku dzanja lamanja la Mulungu (5:1–19:21). Monga bvumbulutso la Yesu Khristu, ladzadzidwa ndi mitu yolongosola bwino, makamaka ikulongosola za Mboni zokhulupirika, oyamba kubadwa kuchokera kwakufa, Wolamulira Mafumu a padziko lapansi (1:5); Woyamba ndi otsiriza (1:17); Iye amene ali ndi Moyo nthawi zonse (1:18); Mwana wa Mulungu (2:18); Woyera mtima ndi woona (3:7); Iye wotchedwa Amen, Wokhulupirika ndi mboni yachilungamo, Chiyambi cha chilengedwe chonse cha Mulungu (3:14); Mkango wa pfuko la Yuda, Muzu wa Davide (5:5); Mwanawankhosa (5:6); Wokhulupirika ndo Woona (19:11); Mawu a Mulungu (19:13); MFUMU YA MAFUMU, MBUYE WA AMBUYE (19:16); Alefa ndi Omega (22:13); Nyenyezi yonyezimira ya Nthanda (22:16); ndi Ambuye Yesu Khristu (22:21).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule

1. **Chiyambi (1:1-8)**
   1:1-3 1:4-8

2. **Zinthu Zakale (1:9-20)**
   1:9-11 1:12-16 1:17-20

3. **Zinthu Zatsopano (2:1–3:22)**
   a. Uthenga ku Aefenso (2:1-7)
   b. Uthenga ku Smurna (2:8-11)
   c. Uthenga ku Pergamo (2:12-17)
   d. Uthenga ku Tiyatira (2:18-29)
   e. Uthenga ku Sarde (3:1-6)
   f. Uthenga ku Filadefiya (3:7-13)
   g. Uthenga ku Laodikaya (3:14-22)

4. **Zinthu za Mtsogolo (4:1–22:5)**
   a. Chisautso chachikuru (4:1–19:21)
      1) Mpando wachifumu Kumwamba (4:1-11)
         4:1-4 4:5-11
      2) Bukhu losindikizika ndi zizindikiro zisanu ndi ziwiri;ndi Mkango/ Mwanawankhosal (5:1-14)
         5:1-5 5:6-10 5:11-14
      3) Chizindikiro cha chiweruzo (6:1-17)
         6:1-2 6:5-6 6:9-11
         6:3-4 6:7-8 6:12-17
      4) Zochitika ziwiri Zosiyana: Owomboledwa pa chisautso chachikuru (7:1-17)
         7:1-3 7:9-12
         7:4-8 7:13-17
      5) Malipenga oyamba Anayi (8:1-13)
         8:1-2 8:8-9 8:13
         8:3-5 8:10-11
         8:6-7 8:12
      6) Lipenga lachisanu ndi lachisanu ndi chimodzi, ndi matsoka awiri (9:1-21)
         9:1-6 9:12
         9:7-11 9:13-19
      7) Ngelo ndi Kabukhu / Yohane adya bukhu lochokera kumwamba (10:1-11)
         10:1-7 10:8-11
      8) Kachisi, Mboni ziwiri, Lipenga lachisanu ndi chiwiri (11:1-19)
         11:1-6 11:11-13 11:15-18
         11:7-10 11:14 11:19
      9) Nkhondo ya Angelo (12:1-17)
         12:1-2 12:5-6 12:10-12
         12:3-4 12:7-9 12:13-17
      10) Chirombo chakuturuka Mmwamba ndi Aneneri onyenga (13:1-18)
         13:1-6 13:7-10 13:11-18
      11) Zolengeza zapadera (14:1-20)
         4:1-5 14:9-12 14:17-20
         14:6-7 14:13
         14:8 14:14-16
      12) Angelo asanu ndi awiri ndi Miliri isanu ndi iwiri (15:1-8)
         15:1 15:2-4 15:5-8

13) Mbale za chiweruzo (16:1-21)

16:1	16:4-7	16:12
16:2	16:8-9	16:13-16
16:3	16:10-11	16:17-21

14) Kupasuka kwa Baibulo/ Chirombo chosokeretsa /Mkazi wa chigololo (17:1-18)

17:1-7	17:8-14	17:15-18

15) Kupasuka kwa Baibulo / Maliro a pa dziko lapansi (18:1-24)

18:1-3	18:9-10	18:21-24
18:4-8	18:11-20	

16) Za kubweranso kwa Khristu (19:1-21)

19:1-4	19:9-10	19:19-21
19:5-6	19:11-16	
19:7-8	19:17-18	

b. Ulamuliro wa Yesu Kristu (zaka chikwi) Mpando waukulu wachifumu (20:1-15)
   1) Satana amangidwa (20:1-3)
   2) Oyera mtima awukitsidwa (20:4-6)
   3) Ochimwa apandukira (20:7-9)
   4) Satana Awonongedwa (20:10)
   5) Ochimwa alangidwa (20:11-15)

c. Moyo wa muyaya (21:1–22:5)
   1) Yerusalemu watsopano / mzinda woyerawo (21:1-8)

21:1-4	21:5-8

   2) Yerusalemu watsopano, maonekedwe ake (21:9-27)

21:9-14	21:15-21	21:22-27

   3) Yerusalemu watsopano, zokondweretsa zake (22:1-5)

d. Mathero: Machenjezano ndi Malonjezano (22:6-21)

22:6	22:12-13	22:18-19
22:7	22:14-15	22:20
22:8-9	22:16	22:21
22:10-11	22:17	

Mutu 4

Ndondomeko Zenizeni za Kumasulira Mau

Malonje

Mutu wachinai walembedwa pofuna kulonjera ophunzira ku mfundo zinai zazikulu ndi zina khumi ndi zisanu za kutanthauzira mau. Mu mutu umenewu, lamulo likutanthauza mfundo zokhazikika zofunikira kwa ophunzira mawu a Mulungu. Mfundo ndi chinthu chimodzi chofunikira cha lamulo limene liri lofunikira kwambiri limene limafunikira kuligwiritsa ntchito koma osati nthawi zonse. Pamene tikupitilira ndi gawo iri la maphunziro,akhala atamvetsetsa za njira zotanthauzira mau komanso nthawi imene angathe kugwiritsa ntchito mfundo zosiyanasiyana zomasulira mau.

Njira yolondola yotanthauzira mau ndi pamene munthu akhala akukhala ndi mtima wotanthauzira mau kwa moyo wake wonse. Palibe njira yokhazikika imene munthu akhonza kutsegula Baibulo, ndipo mu phindi zochepa akhonza kudziwa zimene ndime ina iriyonse ikunena. Ophunzira asakhale odandaula kuti wasiya kufufuza choonadi! Mulungu anaika zinthu zina zovuta mu Mau ake ndi cholinga choti ife tikadalira Mzimu Woyera (1 Akorinto 2:10-16). Pamene ndime zina ndizosavuta kumvetsa, ndime zina sitingathe kumvetsa m'moyo wamuyaya umenewu (1 Akorinto 13:12).

Ngati njira yomasulira Mau a Mulungu ichitika potsata njira ina yake, ndiye kuti munthu osakhulupirira nayenso akhonza kutanthauzira Mau a Mulungu. Mulungu amafuna kuti anthu ake omutsatira, amufune komnaso kuphunzira mau ake monga mbali imodzi ya kukula m'moyo wa uzimu (2 Timoteo 2:15). Chonde gwiritsani ntchito ndondomeko zimenezi monga mfundo zofunikira komanso motsogozedwa ndi Mzimu Woyera amene adzakutsogolereni ku choonadi chonse (Yohane 16:13).

M'munsimu muli chidule cha ndondomeko ndi malamulo oyenera kuwatsatira pamene titanthauzira mau.

Lamulo 1: Funitsitsani kulandira mfundo yeniyeni ya Mulungu ndi Yesu pofunafuna malembo oyera.
A. Mfundo 1: Kufunika kwa Mulungu
B. Mfundo 2: Funisitsani njira yomwe Khristu wauluridwamo.

Lamulo 2: Funitsitsani kumvetsetsa mfundo zofunikira pogwiritsa ntchito nkhani yomveka monga mlezo wanu (chotsogolera).
A. Mfundo 3: Zindikirani kuti mavumbulutso akupitilira
B. Mfundo 4: Masulirani momwe mwawerengera
C. Mfundo 5: Unikirani mfundo zofunikira
D. Mfundo 6: Phunzirani kuchokera mu ndime zapaphataWerengani nkhani yeniyeni
E. Mfundo 7: Zindikirani za umunthu
F. Mfundo 8: Kumbukirani malonjezano

Lamulo 3: Funisitsani kukhala a nzeru pofanizira malembo ndi malembo anzake.
A. Mfundo 9: Onetsetsani Kusiyanitsa
B. Mfundo 10: Wonani nkhaniyo
C. Mfundo 11: Masulirani mofaniza
D. Mfundo 12: Funisitsani chimwemwe
E. Mfundo 13: Kumbukirani kusintha kwa zinthu
F. Mfundo 14: Chenjerani ndi ma uneneri

Lamulo 4: Funisisani kukhala moyo wa chiKhristu poonjezera mawu a Mulungu.
A. Mfundo 15: Kugwiritsa bwino mawu kumachokera pa kumasulira bwino mawu
B. Mfundo 16: Masitepe 4 a kugwiritsa bwino mawu
C. Mfundo 17: Zophinja 6 pa kumasulira kwenikweni
D. Mfundo 18: Njira 8 yolepheretsa kugwiritsa ntchito mawu

Gawo 1
Lamulo 1

Funitsitsani Kulandira Mfundo Yeniyeni Ya Mulungu Ndi Yesu Pofuna Malembo

Lamulori limazindikira zochitika zenizeni za Mulungu, kapena kuti makhalidwe ake monga mfundo yofunikira pokonzera mamasulidwe a Mau. Chimene Mulungu ali sichimasinthika kapena kutsutsidwa. Lamulo iri lakhazikika ponena kuti m'mene ife tiyamikirira komanso kudziwa za ukuru wa chikhalidwe cha Mulungu (Afilipo 3:10), ndi m'mene ifenso tizindikira bwino komanso kukhala ndi luso loti timvetsetse za chimene Iye akufuna kunena.

Chifukwa chonena kuti Mulungu Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera iwo onsewa ali ndi chikhalidwe chofanana, uwu uli ngati umboni woonetsa Utatu woyera monga mwa Baibulo. Mawu oti "utatu woyera" amaimira kuti Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera ali ndi machitidwe a Mulungu m'modzi. Iwowa ali ndi ntchito zitatu. Ntchito ya Atate ndi yopanga mapulani (Mach 2:23), Ntchito ya Mwana ndi yaukhalapakati (Yohane 5:36), ntchito ya Mzimu Woyera ndi ya kuvumbulutsa (Yohane 16:13). Ngakhale ntchito zawo zili zosiyana, koma sitiyenera kuwasiyanitsa pa Utatu Woyera. Pali Mulungu m'modzi (Deut 6:4) popeza Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera onse ali ndi khalidwe limodzi la Mulungu. Onsewa ndi Mulungu m'modzi.

Tiunikira bwino lomwe za Utatu Woyera mwachindunji patsogolo:

A. Lamulo 1: Kuphunzira Kufunika kwa Mulungu

Pali makhalidwe khumi omwe Mulungu ali nawo. Izi zonse ziyenera kulowezedwa komanso kuunikiridwa pafupipafupi.

1. Ulamuliro wonse

Mulungu ndi ulamuliro wonse, kutanthauza kuti Iye ndi mfumu komanso amachita moyenerara. Kukhala ndi mphamvu yonse ndiko kukhala ndi ulamuliro wochuluka pa malo ochepa. Mulungu al indo pa Iye yekha, osati zochokera kwina ndi kwina, Iye ali ndi ulamuliro pa chilengedwe chonse. Iye ndi mlengi, osati olengedwa (Aroma 1:20, 25). Choncho ali ndi ulamuliro wokhazikitsa mapulani ake, malamulo ake komanso chiweruzo chake. Mwachidule Iye ali ndi ulamuliro wochita monga akufunira kuchita, ngakhale kuti zolinga zake pena sungathe kuzimvetsa.

2. Chilungamo

Mulungu ndi wachilungamo chonse, kusonyeza kuti ndi wangwiro munjira zonse. Iye ndiye mulingo wa chilungamo kumbali zonse. Iye alibe banga, ndipo akupereka muyeso wa chikhalidwe choti tikhalemo (Aefeso 5:1).

3. Choonadi

Mulungu ndi Choonadi, kutanthauza kuti alibe kukondera kwina kulikonse. Choonadi cha Mulungu ndi yankho kuchokera ku chilungamo chake. Mulungu samasamala za munthu pochita ziganizo (Aroma 2:11); Iye alibe tsankho. Pamene pali tchimo (Aroma 5:13), chilungamo chake chiyenera chikwanilitsidwe.

4. Chikondi

Mulungu ndi chikondi, kutanthauza kuti ndiwopanda banga komanso wachikondi chake ndichopanda malire. Chikondi chimaimilira kuchita zabwino kwa ena ngakhale iwo apange zosayenera kwa iwe. AKhristu ayenera kukhala ndi chikondi cha Mulungu ndi kufalitsa kwa ena kuti azindikire Mulungu (Yohane 13:34-35).

5. Moyo Wosatha

Mulungu ndi moyo wosatha. Iye wakhalapo ndi adzakhalabe wamuyaya. Moyo wosatha ulibe chiyambi komanso chimaliziro. Ife monga akhristu tiri ndi moyo wosatha, umene uli ndi poyambira, koma ulibe chimaliziro. Moyo wosatha wa Mumulungu, umatiphunzitsa kuti Mulungu sangathe kufa.

6. Wamphamvu yonse

Mulungu ndi wamphamvu zonse, kutanthauza kuti ali ndi mphamvu yochita zirizonse. Chitsanzo cha mphamvu ya Mulungu chikuonekera pa chilengedwe cha dziko la m'mwamba ndi lapansi (Genesis 1:1). Timamva kuti "mawu a pakamwa pake" analenga zones ndi "mpweya" wake (Masalmo 33:6).

7. **Wopezeka Paliponse**
   Mulungu ndiye wopezeka paliponse. Izi zikusonyeza kuti chilichonse chomwe timachita amachiona mu nthawi zonse. Izi sizikutanthauza kuti Mulungu ndi chinachirichinso (Pantheism), koma kuti ali paliponse. Lingaliro iri limationetsa za chikhalidwe cha umunthu wa Mulungu.

8. **Wodziwa Zonse**
   Mulungu ndi wodziwa zonse. Iye amadziwa zochitika zonse mu nthawi yakale, yatsopanao, ndi yamtsogolo. Mulungu amadziwa zinthu zonse zobwera osangokhala zochitika zenizeni komnaso zimene zikhonza kuchitika mu nthawi ina. Iye amadziwa zonse zimene zimadza kamba ka zinthu zina mu nthawi zonse, komanso ndi ganizo lina lirilonse limene lingabwere. Mapulani ake a muyaya alumikizana ndi zinthu zonsezi (Aroma 8:28-30).

9. **Wosasintha**
   Mulungu ndi osasintha zimene zikutanthauza kuti chikhalidwe chake ndichosasintha.

10. **Wachoonadi**
    Mulungu ndi choonadi chenecheni Chikhalidwe chimenechi chimatiuza kuti zonse zimene Mulungu amanena ndizoona ndinthu ndipo ndizoyenera kuzikhulupirira (Numeri 23:19). Ndipo ndi zinthu zoona kuti Mulungu sanganame (Tito 1:2).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Chaputala 4, Gawo 1A

1. **Lowezani makhalidwe khumi a Mulungu amene aperekedwa.**

2. **Werengani Masalmo 11, ndipo pezani makhalidwe ena ambiri amene mukhoza kuwapeza**

B. Lamulo 2: Funafunani Njira Yomwe Khristu Waululidwamo

Lamulo lachiwiri likuonetsa kuti mbiri yonse ikulozera kwa Yesu Khristu. Lamulo iri likuonetsa kuti Yesu Khristu ndi mlengi wa zonse (Yohane 1:1, 3, 14; Akolose 1:16-17), Alefa ndi Omega, "Chiyambi ndi mathero" (Chibvumbulutso 1:8), Mulungu yekhayo amene anakhalapo munthu (Afilipi 2:6-8).

Pamene tikufuna kumvetsa mau a Mulungu, tiyenera kuti tionesetse kuti pamene timasulira ndime ikulumikizana bwino ndi Choonadi cha Ambuye Yesu Khristu. Njira imodzi yopangira izi ndikuzindikira zinthu munthu aliyanse, malo, chinthu, kapena chochitika china mu malemba kuti chikuphunzitsa chiyani chokhudza Ambuye. Ife tikulimbikitsidwa kuphunzira komanso kuyang'ana "zinthu zabwino" (choonadi chenicheni, cha Ambuye Yesu Khristu), osangoyang'ana ku Lamulo lakale limene linari "chithunzithunzi cha zinthu zabwino izi" (Ahebri 10:1, Yohane 14:6). Anthu onse, malo onse ndi zochitika zonse za m'Chipangano Chakale zinaikidwa ndi Mulungu monga chitsanzo chothandiza ife kuti tiphunzire za Iye (1 Akorinto 10:1-6).

Chitsanzo cha ***munthu*** wophunzitsa ife za Ambuye amaoneka monga mneneri Yona. Monga tikudziwa, Yona sanafune kupita ku Asuri monga anatumidwa ndi Mulungu. M'Malo mwake anakwera chombo napita kwina. Ndipo namondwe atakula, Yona anaponyedwa m'madzi. Yona anemezedwa ndi nsomba, ndipo patapita masiku atatu, anasanzidwa ndi nsomba ija ku Asuri kumene iye anamvera zimene malamulo a Mulungu. Masiku atatu ndi usiku utatu anatchulidwa "chizindikiro cha Yona" (Mateyu 12:39-40), zimene zikuvumbulutsidwa ngati nthawi imene Yesu adzakhale m'mimba.

Malo angathenso kuphunzitsa za Ambuye. Yesu anabadwa ku Betelehemu (Mika 5:2) kutanthauza "nyumba ya m'kate." Yesu anali m'kate wochokera kumwamba (Yohane 6:35). Pali zinthu zambiri zopangidwira ambuye. Likasa ndi kachisi ziri mu gulu limeneli. Tikaona malo oyera ndi gome la golide zinali ndi malo ake kuimira Yesu (Yohane 6:35) kuunika kwa dziko (Yohane 8:12; Chiv 8:3-4; Ahebri 13:15-16).

Pali ***zinthu*** zambiri zochitika zimene zikhonza kutiphunzitsa za Ambuye. Chihema ndi Kachisi zikuonekera mu gawo iri. Ngati tikhonza kuona za malo oyera a pagome la mkate, zoimikira nyali, pamene panali guwa la nsembe zopsereza izi zonse zimatiphunzitsa za Ambuye (Lev 1-7) kuti Iye ndi mkate wamoyo (Yohane 6:35). Iyenso ndi "kuunika kwa dziko lapansi" (Yohane 8:12) komanso amene amamva mapemphero athu. (Nsembe zofukiza zimaimira mapemphero a oyera mtima [Chivumbulutso 8:3-4], ndipo pemphero ndi msembe [Ahebri 10:10-12].

Zochitika, zina monga ngati nsembe zoperekedwa ndi ansembe, zimatiphunzitsanso za Ambuye. Nsembe zonse zoperekedwa (zimene zafotokozedwa mu Levitiko 1-7) izi ndi zinthu zimene zaonetsedwa kwa ife

zimene zikulosela Yesu monga “wodzipereka kamodzi nsembe monga ya kwa onse” (Ahebri 10:10-12). Yesu anali ***“mwana wa nkhosa wochotsa machismo a dziko lapansi”*** (Yohane 1:29).

Ophunzira ayang’anenso mitu mu bukhu lirilonse ndipo awone kuti Yesu Khristu ndi mutu weniweni.[98]

Genesis	Mlengi ndi nsembe ya mzimayi (1;1; 3:15)
Eksodo	Mwana wankhosa wa Mulungu woperekedwa chifukwa cha tchimo (12:1-13)
Levitiko	Mkulu wa nsembe (mabuku onse)
Numeri	Nyenyezi yochoka pa Yakobo (24:17)
Deutronomo	Mneneri wonga onse (18:15)
Yoswa	Mkulu wa Ambuye wamakamu (5:13-15)
Oweruza	Oweruza (11:27)
Rute	Woombola (3)
Samueli	Mbuye wa mafumu (2 Samueli 7:18-20)
Mafumu/Mbiri	Ambuye wa kumwamba ndi dziko (mabuku onse)
Ezara	Wobwezeretsa (1:1)
Nehemiya	Wokhulupilika (9:32)
Esitere	Woyenera (10)
Yobu	Wokwera (19:25)
Masalimo	Munthu wodalitsidwa (1)
	Mwana wa Mulungu (2)
	Wopachikidwa (22)
	Wokwera (23)
	Wobwerayo (24)
	Wolamulirayo (72)
	M’sogoleri wa matamando (150)
Miyambo	Nzeru (4)
Mlaliki	Wanzeru woiwalidwa (9:14-15)
Nyimbo ya soloimo	Wokondedwa wanga (2:16)
Yesaya	Wozunzika m’malo mwathu (53)
Yeremiya	Ambuye wa choonadi (23:6)
Maliro	Munthu wazisoni (1:12-18)
Ezekieli	Wokhala pa mpando wachifumu (1:26)
Danieli	Mwala woponyedwa (2:34)
Hoseya	Mfumu yaikulu ya Davide (3:5)
Yoweli	Ambuye wakukoma (2:18-19)
Amosi	Wopulumutsa Israyeli (3:12)
Obadiya	Momboli wa Zioni (17)
Yona	Woikidwa m’manda ndi kuukanso (bukhu lonse)
Mika	Mulungu wa muyaya (5:2)
Nahumu	Wamphamvu pa tsiku la chidzudzo (1:7)
Habakuku	Wogwira chikhulupiliro chathu (2:4)
Zefaniya	M’kati mwa chiweruzo ndi woyeretsa (3:5, 15)
Haggai	M’busa wokanthidwa (2:17)
Zekariya	Nthambi (3:8)
Malaki	Dzuwa la chilungamo (4:2)
Mateyu	Mfumu ya a Yuda (2:1)
Marko	Kapolo wa Yehova (bukhu lonse)
Luka	Mwana wa munthu wopanda banga (3:38; 4:1-13)
Yohane	Mwana wa Mulungu (1:1)
Machitidwe	Ambuye wokwera (1:8-9)
Aroma	Choonadi (3:22)
1 Akorinto	Chipatso choyamba kucha (15:20)
2 Akorinto	Wopangidwa tchimo m’malo mwathu (5:21)
Agalatiya	Kutha kwa lamulo (3:10, 13)
Aefeso	Lupanga lathu (6:11-18)
Afilipi	Wopereka zosowa zathu (4:19)
Akolose	Wamuyaya (1:18)
1 Atesalonika	Ambuye wobwerera (4:15-18)
2 Atesalonika	Kubwerera kwa dziko kwa oweruza (1:7-9)
1 Timoteo	Mkhalapakati (2:5)
2 Timoteo	Wopereka korona (4:8)
Tito	Mulungu wamkulu ndi Mpulumutsi (2:13)

Filimoni	Bwenzi la andende (1:9)
Ahebri	Mpumiro wa chikhulupiliro (9-11)
Yakobo	Ambuye wamphamvu yonse (5:4)
1 Petro	Mutu wa uneneri wa chipangano chakale (1:10-11)
2 Petro	Mpulumutsi wopilira zowawa (3:9)
1Yohane	Mau amoyo (1:1)
2 Yohane	Kutsutsana ndi okana Khristu (1:7)
3 Yohane	Choonadi cha munthu aliyense payekha (1:3-4)
Yuda	Chitetezo cha okhulu (1:24-25)
Chibvumbulutso	Mfumu ya mafumu, Mbuye wa Ambuye (19:11-16)

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Chaputala 4, Gawo 1B

1. **Werengani Yohane 1:1, 3 ndi 14; Akolose 1:16-17 ndi Afilipi 2:6-8. Kodi Yesu Khristu ndi ndani?**

2. **Werengani Ahebri 10:1-18 ndi 14:6.Kodi chimachotsa machismo ndi chiyani? Ndani angachotse uchimo?**

3. **Werengani Mateyu 12:39-40 ndi Yona. Lembani kufanana kwa yona ndi Yesu Khristu.**

4. **Werengani Mika 5:2 ndi Yohane 6:32-51.Kodi mau awa akuulula motani za Yesu Khristu.**

5. **Werengani Eksodo 25:23-40, Yohane 6:35 ndi 8:12. Kodi kukongoletsa likasa kumatanthauzanji za Khristu Yesu?**

6. **Werengani levitiko 3, Ahebri 10:10-12 ndi Yohane 1:29. Kodi nsembe ya mtendere ndi Yesu Khristu zikufanana motani ?**

7. **Onani mavesi onena za Yesu Khristu ndipo onani chinthunzi cha Khristu pa inu?**

Gawo 2
Lamulo 2

Funafunani Kumvetsetsa Zoonadi Pogwiritsa Ntchito Gawo lolondora la Mlozo Wanu

Lamulo iri likutiphunzitsa za kuona malembo omwe ndi osavuta kumvetsa kuti akhale mlozo wanu pomvetsetsa malembo amene ovuta kuwamvetsa. Tidzaphunzira mfundo zisanu ndi imodzi zokhudzana ndi lamulo iri. Mfundo zimenezi zidzathandiza ophunzira kupeza ndi kuunikira ndime zimene zakhazikitsa ndi kufotokoza za maphunziro ena ndi ena opezeka mu malemba.

A. Mfundo 3: Zindikirani kuti Bvumbulutso Likupitilira

Mfundo iyi imatiphunzitsa kuti Mulungu amaulura mfundo pa nthawi yake. Mwachitsanzo, ulosi woyamba wa Mesiya ukupezeka ku Genesis 3:15, ndi ulosi wumbeu yolonjezedwa ya mkazi. Chipangano Chakale chonse chikupitilira kuperekabe nkhani yokhudza mbeu. Ife tikuuzidwa kuti Mesiya ameneyu adzachokera ku mbeu ya Abrahamu (Genesis 12:3), mbeu ya Isake (Gen 21:12), mbeu ya Yakobo (Gen 35:10-12), wa fuko la a Yuda (Gen 49:8-11), mbumba ya Jesse (Yesaya 11:1), ndi wa mnyumba ya Davide (2 Samueli 7:12-16). adzabadwa mu Betelehemu (Mika 5:2). Iye adzakhala Mulungu komanso munthu (Masalmo 110:1). Ndipo adzatchulidwa kuti Emmanueli (Yesaya 7:14). Iye adzakhala mneneri (Deut 18:8), wansembe (Masalmo 110:4), woweruza (Yesaya 33:22), mfumu (Yesaya 22:5). Ndipo iye adzakhala ndikudzoza kwa Mzimu Woyera kwapaderadera (Yesaya11:2), komanso adzakhala ndi chidwi chonse pa nyumba ya Mulungu (Masalmo 69:9). Mabvumbulutso akufotokozedwa mwakuya pamene nthawi ikupitilira, (monga ngati ochokera kumwamba) ndipo akutchulidwa kuti ndi "bvumbulutso lopitilira". Bvumbulutso la kwa onse laperekedwa komanso zinthu zofunikira kwmabiri za bvumbulutsolo zaululidwa pamene nthawi ikupitilira.

Choncho ndizinthu zomveka kwambiri kuti poyambirira tiyambe taona kaye za phunziro lina,ndipo iri lithandizire ife kumvetsetsa zochitika zina zimene zikubwera zokhudza phunziro lomwelo. Monga mwa chitsanzo, ntchito ndi kuchenjera kwa Satana zikuoneka mu Genesis 3:1. Pamene ife tiphunzira za "njoka", ife tikudziwanso kuti iyeyo ndiye wonyenga komanso otsutsa weniweni wa Mulungu. Satana samasintha kukhala munthu wabwino mu mbiri yake yonse (Chibvumbulutso 12:9; 20:7-8) komanso machitidwe ake a zinthu amapitilirabe kufuna kukhala ka mulungu koima pakokha. Izi zikufotokozedwa bwino pame "munthu wosaweluzika" watenga mpando wake ndikukhala mu Kachisi panthawi ya Chizunzo ndipo iye amadzitchula yekha kuti ndiye mulungu (2 Atesalonika 2:4).

Mu nthawi zambiri timapeza choonadi pa chimene chaperekedwa pa mutu wina, chikuphunzitsidwa mogwirizana ndi kutchulidwa kwake pamayambiriro. Komanso, mitu yambiri yopezeka mu Baibulo yakambidwa mu bukhu la Genesis. Mosamalitsa, munthu ngati awerenga mosamalitsa komanso mwachidwi chake chonse, bukhu la Genesis akhonza kumasulira bwino Mau a Mulungu, ndipo izi ndi zinthu zabwino kwambiri.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Chaputala 4, Gawo 2A

1. **Werengani Mateyu 1:1-25; 2:1; 3:16; Yohane 1:1, 14; 2:17; Ahebri 5:9-10 ndi Chibvumbulutso 19:16; 5:22; 7:40 linganizani mawu ndi vesi yake pa uneneri wa Yesu.**
   a. Mbeu ya mkazi-Gen 3:15
   b. Mbeu ya Abrahamu-Gen 12:3
   c. Mbeu ya isaki-Gen 21:12
   d. Mbeu ya yakobo-Gen 35-10-12
   e. Pfuko la ayuda-Gen 49:8-11
   f. Mbumba ya jesse-Yesaya 11:1
   g. Nyumba ya davide-2 Samueli 7:12-16
   h. Wobadwa ku bethlehemu Mika 5:2
   i. Mulungu ndi munthu-Masalmo 110:1
   j. Wotchedwa emmanueli-Yesaya 7:14
   k. Mneneri- Deut 18:18
   l. Wansembe-Masalmo 110:4
   m. Woweruza- Yesaya 33:22
   n. Mfumu-Yesaya 22:5
   o. Kudzoza kwa Mzimu Woyera- Yesaya 11:2
   p. Changu mu nyumba ya Mulungu-Masalmo 69:9

2. **Kodi mavesi awa akutsimikizira zotani?**

B. **Mfundo 4: Masulirani Monga Mwawerengera**

Mfundo iyi imatiphunzitsa kuti Mulungu amanena zomwe akutanthauza ndipo amatanthauza zomwe akunena (Ahebri 1:1). Iyi ndi mfundo yofunikira kwambiri chifukwa imatitsogolera kuti timvetsetse Mau a Mulungu. Pamene tilangiza ana athu, timayesera kulumikizana nawo bwino pa zinthu zomwe timafuna kuti akumbukire. Nthawi zambiri timakambirana zinthu mu njira zosiyanasiyana ndicholinga chakuti iwo amene ali ndi malingaliro aang'ono akhonze kumvetsetsa komanso kuti astaye zimenezo (Ahebri 1:1). Ndipo ife tidzapitiliza kubwereza uthenga womweo kangapo konse. Kodi ife si ana a Mulungu (1 Yohane 3:1)? Kodi iye si atate athu ABBA (Aroma 8:15). Kumasulira kwa zinthu monga m'mene ziriri zikutanthauza kuti ife (monga ana a Mulungu) tavomereza choonadi cha Mulungu monga m'mene alembera mu Baibulo. Izi ziri zinthu zomveka kuti ife anthu tiyang'ane Mau amene ali ophweka, omveka, achindunji komanso, okhudza anthuonse. Mwachidziwikire kuti, ndime zina zimene ziri zovuta, zikohnza kuunikira za ndime zina zovutirako.

Chitsanzo china chosavuta, chomveka bwino komanso chachindunji chikupezeka mu Yohane 3:16 ***"Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kuti anampatsa mwana wake wobadwa yekha kuti yense wakukhulupilira iye asatayike koma akhale nawo moyo wosatha."*** Palibe mau okaikira pa chikondi cha Mulungu, monga "mwina", "kapena", kapenanso "monga". Ndime ikuonetseratu mwachindunji za chikondi Chake ku dziko lapansi, komanso akunena kuti "yense wakukhulupirira" akhale nawo moyo wosatha. Zimene Mulungu sakufotokoza kwambiri zitiuza ifenso kuti tisaonjezere.

Tikupeza mau enanso ofanana ndi amenewa mu Aroma 3:23 ***"pakuti onse anachimwa naperewera ku ulemelero wa Mulungu"***. M'mene tchimo lirili molingana ndi Baibulo, limakhudza anthu onse – kupatulapo Yesu Khristu (Petro 2:22).

Baibulo palokha limatsimikiza za limanena mfundoyi, ndi chifukwa chake kuti Baibulo lokha likhonza kutsimikiza za mfundo imeneyi. Ife monga ophunzira tilibe ufulu wokana zinthu zimene Mulungu wazikamba koma ziri zokhudza anthu onse. Choncho kupatula Yesu Khristu, tonse ndife ochimwa. choncho opanda Khristu ndi ochimwa

Ndi mwachidziwikire kuti kungoganiza za matanthauzo a mau "obisika" komanso "amene ali ozama" pa malemba ndi kulephera kukhala ndi udindo pa Mau a Mulungu. Monga takambira kale, njira younikira zinthu zimene ziri ndi tanthauzo lobisika pomasulira mau, izi zimayesa kuonjezera mau a Mulungu. Komanso njira younikira nkhani zopeka, imayesera kuchotsa choonadi pa mau a Mulungu. Mulungu watichenjeza ife ndithu pazinthu zotere (Chibvumbulutso 22:18-19), chifukwa zimachotsa tanthauzo la mau a Mulungu monga m'mene aliri.

Baibulo lakhazikika pa mbiri monga m'mene iriri, komanso mbiri imeneyi ndiyofunikira ku mbiri yonse (onani 1 Akorinto 15). Kulephera kutenga tanthauzo la mau monga m'mene aliri zapangitsa kuti anthu ambiri aononge tanthauzo la za uMulungu, mu mbiri ya Israyeli komanso mpingo.

Zitsanzo za mbiri za zinthu zimene zokamba za anthu onse, zimene tiyenera kutanthauzira monga m'mene ziriri ndi: Aroma 8:33-39; Yohane 3:16, 18, 36; Aefeso 2:8-10; 1 Yohane 2:1-2 ndi Tito 3:5.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Chaputala 4, Gawo 2B

1. **Lembani mfundo mu mawu awa**
   a. Aroma 8:35-39
   b. Yohane 3:16
   c. Yohane 3:18
   d. Yohane 3:36
   e. Aefeso 2:8-10
   f. 1 Yohane 2:1-2
   g. Tito 3:5

2. **Lingalirani zomwe mavesi akutanthauza kwa inu ndi okondedwa anu. Kodi mukukhulupilira izi?**

C. Mfundo 5: Unikirani mfundo zofunikira

Mfundo iyi imazindikira kuti pali mafunso ofunikira oti ayankhidwe pamene tikumasulira mawu a Baibulo. Mwachitsanzo, tiyenera kufunsa kuti "ananena izi ndi ndani"? kodi zinanenedwa kwa ndani? Ndipo m'mene zimanenedwa pamachitika chiyani? Kodi nanga izi zikukhudza ndani?

Mfundo imeneyi imazindikiranso kuti Mulungu wagwira ntchito ndi magulu a anthu atatu, mu mbiri, amenewa ndi Ayuda, Amitundu komanso Mpingo. Ndipo ife tiyenera kudziwa kuti kodi izi zikulembedwera ndani, amene amalandira mbali ya malembawo, kuti ife tidziwe kuti kodi ndi lonjezo, pangano kapena chenjezo limene likutikhudza.

Ndipo ife tiona pamene tikuphunzira za mapangano maka kuti ndi kwa ndani kumene pangano likupita chifukwa izi ndi zofunikira. Mwa chitsanzo fuko la amitundu, (limene siriri fuko la Ayuda) akhonza kuchotsedwa kapena kumwazidwa chifukwa cha uchimo komanso kusamvera kwa Ambuye. Anthu a kuSumeriya, a Babulo, Asuri ndi a Aperezi, ndi ena mwa mafuko (anthu) amene izi zinayamba zawachitikira.

Mulungu sanangonena kuti adzawabalalitsa a Israyeli kokha, komanso adzawasonkhanitsanso. Palibe mtundu wa anthu umene unalandira lonjezo iri. Tikhala kuti tatenga malonjezo amenewa ndi kuwapereka kwa anthu ena, amene anaperekedwa kwa a Israyeli, tikhonza kulakwitsa.

Chitsanzo chachiwiri ndi lonjezo la dziko, malo komanso unzika wa a Israyeli mu Kanani (Genesis 12:1-3; 13:15), koma unzika wakumwamba umene uli wa Mpingo (Aafilipi 3:20). Nkhani ya malo sinalonjezedwe kwa mpingo.

Chitsanzo chotsiliza chikusiyanitsa m'dalitso wa Israyeli pokhala pa ubale ndi Mulungu (Deut 8:7-10) ndi m'dalitso wa Mulungu pa mitundu podalitsa a Israyeli (Genesis 12:3). Palibe madalaitso kwa iwo amene adalitsa mpingo kapena amitundu.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Mutu 4, Gawo 2C

1. **Werengani Genesis 12:1-3. Kodi Mulungu akulonjeza kuti adzadalitsa ndani?**

2. **Werengani Genesis 12:1. Tchulani zoyenereza omwe zinalipo kuti Mulungu adalitse Abrahamu?**

3. **Werengani Genesis 26:5. Chifukwa chiyani Mulungu anadalitsa Isake?**

4. **Werengani Ahebri 11:8. Chifukwa chiyani Abrahamu anamvera Mulungu?**

5. **Kodi malamulo omwe anaperekedwa kwa Abrahamu mu #2, ndi ofunikirabe motani ku mpingo walero?**

6. **Kodi madalitso omwe anaperekedwa kwa Abrahamu analonjezedweranso ku mpingo walero?**

7. **Werengani Agalatiya 3:28-29. Kodi tingapeze nawo Madalitso a Abrahamu?**

D. Mfundo 6: Phunzirani kuchokera mu ndime zapaphata

Mfundo iyi imazindikira kuti ndime zina ziyenera kuwerengedwa ngati monga pa phata lake, komanso ndi m'mene Mulungu analengezera pa phunziro limenelo limene liri lofunikira ku moyo wahtu wauzimu. Mu nthawi zambiri mu Baibulo, Mulungu amasonkhanitsa zidutswazidutswa za nkhani yachoonadi zimene ndipo amaziika pamodzi mu zina mwa ndime izi:

- Kuukanso kwa Yesu–1 Akorinto 15
- Malilime a anthu–Yakobo 3
- Kubwereranso kwa chikhulupiliro–Aroma 11
- Kukondwera mwa chikhulupiliro–Ahebri 11
- Chilango cha Mulungu pa anthu–Ahebri 12:1-11
- Mpingo–Aefeso 1-3
- Chilungamo mwa chikhulupiliro–Aroma 3:10-21
- Chilamulo–Eksodo 20
- Zida za Mulungu–Aefeso 6:10-17
- Chikondi-1 Akorinto 13

Mfundo iyi imafuna ife tiphunzire malemba a paphata enieni kuti tidziwe mfundo zikuruzikuru komanso kuona ndime zina zimene zikhonza kutithandiza kupeza nkhani zoonjezera.

Mwa chitsanzo, ndime imene yaikuru kwambiri mu baibulo ndi imene ikupezeka pa 1 Akorinto 13:4-8a, pamene pali mfundo khumi ndi chisanu ndi chimodzi zokamba m'mene chikondi chimaonekera:

> ***chikondi chimapilira, chilichokoma, chopanda kaduka, sichizitama, sichichita zosayenera, sichisata za mwini yekha, sichipsa mtima, sichisinjira zoipa, sichikondwera ndi chinyengo koma chikondwera ndi choonadi. Chikwirira zinthu zonse, sichitha nthawi zonse.***

Tikawerenga Marko 12:29-31 tipeza kuti Yesu anayankha funso lokhudza lamulo loposa onse:

> ***Lamulo loposa ndi ili, mvera Israyeli a mbuye Mulungu wathu, ambuye ndiye m'modzi. Ndipo udzikonda ambuye Mulungu ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zones, ndi mphamvu zako zonse. Lachiwiri ndi ili uzikonda mnzako monga uzikondera iwe mwini, palibe lamulo loposa awa.***

Pozindikira kuti malamulo awiriwa akukhudza zaubwino wachikondi, komanso kufunitsitsa kudziwa zimene ziri mu chikondi – ndi cholinga choti tidzisanthule tokha pamaso pa Mulungu ndi anthu, zimene ziri zinthu ziri zabwino. Kufunikira kwa chikondi kukupezeka pa Marko 12. Ndiponso chionetsero chake chiri mu 1 Akorinto 13.

Ngati inu mukufuna kuyesa m'mene chikondi chingakukhudzireni pamoyo wanu, monga zalembedwera mu 1 Akorinto 13, dzifunseni nokha uti udzindikire wekha ngati uli ndi chikondi, uyenera kudzifunsa kuti, "kodi ndimapilira?" "ndiri ndi chifundo?" "nanga ndilibe nsanje?"

Chitsanzo china chokhudza mfundo imeneyi chikufotokozeredwa pa "zida za Mulungu" (Aefeso 6:10-17). Awa ndi malo okhawo amene zida za Mulungu zatchulidwa pamodzi. Lamba limene munthu amadzimanga "la muchunu la choonadi" likutchulidwa mu Yesaya 11:5. Chapachifuwa ndi chisoti zikutchulidwa pa 1 Atesalonika 5:8. Lupanga monga mwa chida chimodzi chatchulidwa pa Ahebri 4:12.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Chaputala 4, Gawo 2D

1. **Werengani 1 Akorinto 15, ndipo lembani moyenera**
   a. 15:1-11
   b. 15:12-19
   c. 15:20-28
   d. 15:29-34
   e. 18:35-49
   f. 15:50-58

2. **Werengani 1 Akorinto 15:3-5, Tchulani zinthu zofunika pa uthenga wa chipulumutso?**

E. Mfundo 7: Zindikirani za mphamvu ya munthu yopanga zinthu

Lamulo ili limazindikira za ufulu omwe Mulungu wapereka kwa munthu wopanga zisankho komanso ndi udindo umene umadza kamba ka ufulu umenewu (Yohane 3:18; Agalatiya 6:7). Mfundo yachisankho chathu monga anthu chikuonetsedwa pamene Adamu ndi Hava anayesedwa mu Genesis 2-3. Chifukwa choti Mulungu amadziwa zonse, Mulungu anadziwa kuti iwo ***"adadya cha mtengo wodziwitsa chabwino ndi choipa"*** koma Mulungu sanali obweretsa za chakudya choletsedwachi. Adamu ndi Hava anadya chipatso cha mtengo oletsedwa, chifukwa iwo anasankha kutero. Iwowa anakhala adindo chifukwa cha zimene anapanga, ndipo anachotsedwa m'munda wa Edeni.

Pali mau ambiri amene amalozera mwachindunji za kusankha kwa munthu – makamaka mau oti "kukhulupirira" ndi "chikhulupiriro" amene ali ndi mau ofanana kuchokera ku chilankhuro cha chiGiriki. Chifukwa chakuti Mulungu amadziwa zonse, Iye wakhala akudziwa za amene angakhulupirire mwa mwana wake Yesu Khristu komanso ndi kupulumuka (Aroma 8:29; 1 Petro 1:1-2). Kudziwa kwake kwa zinthu ngakhale zamtsogolo, sikumapangitsa kuti anthu asamukhulupirire.

Baibulo linalemba zisankho za anthu zabwino ndi zoipa zomwe. Ndipo izi ziri ngati umboni wa ife umene umakhala mkati mwathu. Ife timazindikira bwino za mfundo imeneyi kuti Mau a Mulungu, analemba za ziganizo zoipa za anthu. Izi ndi zinthu zaufulu zimene munthu amachita zimene zinaloledwa ndi Mulungu ndi cholinga cha mapulani ake, koma sizinalamulidwe ndi Iye. Chifukwa chakuti baibulo lalemba kuti munthu akhonza kuchita chinachirichonse koma sizikutanthauza kuti Mulungu wavomereza. Yesu Khristu anadziwa

kuti adzamupereka Iye, komnaso Yudase anachenjezedwa pankhani imeneyi (Mateyu 26:24), koma Yudase anampereka Yesu ndipo iye analandira zotsatira zake.

Mulungu anatipatsa mwayi wosankha nthawi zonse, koma osati kuti kusankha kwathu kuli kwabwino nthawi zonse. Choncho tiyenera kuona zisankho zoipa ndi zauchimo za anthu pamene timasulira mau.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Chaputala 4, Gawo 2E

1. **Yohane 3:16-18. Munthu angatani kuti asalandire chilango?**

2. **Aroma 3:21-26. Munthu angatani kuti alandire choonadi cha Mulung?**

3. **Genesis 2-3. Anthu sanamvere Mulungu kodi?**

4. **Kusamvera kukuoneka pati?**

5. **Werengani Yakobo ndipo mupeza malamulo 60? Lamulo lina lirilonse limafuna kuti ganizo lipangidwe ndi munthu amene akulandira malamulo. Choncho, kodi lamulo lirilonse likuimira chiyani?**

F. Mfundo 8: Kumbukirani Mapangano

Mfundo iyi imazindikira za mgwirizano (kapena kontrakiti) pakati pa Mulungu ndi munthu. Awa ndi mapangano amene akuonetsa kuti munthu achitepo kanthu, komanso pali mapangano ena amene akudalira ndithu pa choonadi cha Mulungu.

Mapangano ndi ofunika chifukwa amatipatsa ife chithunzithunzi cha mbiri molingana ndi m'mene Mulungu amalumikizirana ndi anthu ake. Ngati timvetsa mapangano a Mulungu, ndikulora kuti mapangano amenewo atitsogolere ife tidzakhala anthu otetezeka ku kumasulira kolakwika kwa Mau a Mulungu amene akuoneka kukhala ovutirapo. mwachitsanzo ana a Israeli analangidwa mu mbiri ndi zinthu zambiri zovuta komanso chiononogeko (Levitiko 26) komabe iwo santethedwe chifukwa Mulungu anawalonjeza kuti adzawateteza.

Pali malonjezano 9 amene munthu ayenera kuphunzira. Ife tiyenera kuonetsa za mitu yake komanso kufotokozera pang'ono za pangano lirilonse poperekanso ndime zake za m'baibulo.

1. **Pangano la Eden**

   Pangano la Eden inapangidwa m'munda mwa Eden pakati pa Adam ndi Mulungu (Genesis 1-2). Iri linali pangano loti munthu achitepo kanthu ndipo linari ndi maziko pa kumvera kwa munthu, komanso linari ndi lonjezo lopita kwa munthu pomudalitsa iye ndi malo abwino kwambiri (2:8), chakudya chabwino, kuona zinthu kwabwino (2:9), nyengo yabwino (1:6-7; 3:8), kugonana kwabwino (2:21-28), komnaso kuyanjana ndi Mulungu tsiku ndi tsiku (1:26-27; 3:8).

   Pangano linalandilidwa ndi munthu koma anaononga chimene Mulungu anachikhazikitsa pophwanya pamene anadya mtengo woletsedwa. Pangano la Eden lilibenso mphamvu tsopano chifukwa chifukwa chakuti ambiri a madalitso a munthu adzabwera mu nthawi yamtsogolo pamene Kumwamba ndi Dziko lidzakonzedwa kwatsopano(Chibvumbulutso 21–22). Choncho ife sitiyenera kumasulira za lonjezano iri mosemphana ndi zinthu zimene zimachitika m'munda mwa Eden. Anthu onse sangathe kulandira madalitso onse olonjezedwa popanda Yesu Khristu.

2. **Pangano la Adamu**

   Pangano la Adamu linapangidwa pakati pa Mulungu ndi Adamu m'munda iye atachimwa koma asanathamangitsidwe (Genesis 3:14-19). Pangano ili linali lakuti iye sanayenera kuchitapo kanthu.

   Pangano linabwera kamba ka chilango pa tchimo loyambirira lotchedwa "Kugwa". Mulungu anatembelera chida chonse chopangitsa anthu chinyengo (3:14),komanso nabweretsa udani mu mibir pakati pa zidzukuru za Adamu ndi njoka (3:14-15).Ndipo mkazi anapatsidwa ululu pobereka kwa komanso kuti adzakhala omvera munthu wa m'muna(3:16). Nthaka inatembereredwa (3:17-19), imene idzakhala ndi mavuto popereka chakudya. Mamuna ndi mkazi adzafa thupi (3:19; 2:17) ndiponso anachotsedwa mu Eden (3:17-19).
   Pangano ili lilipobe mpakana nthawi yomwe Mulungu adzaponye satana mu Nyanja ya moto zitatha zaka chikwi (Chibvumbulutso 20:7-9). Choncho uchimo wa Adamu umapita ku mitundu ya anthu osiyanasiyana (Aroma 5:12-14).

3. **Pangano la Nowa**
Pangano la Nowa limene likupezeka mu Genesis 8:20; 9:17, linapangidwa pakati pa Nowa ndi Mulungu chitatha chigumura. Iri ndi pangano limene Nowa sanayenera kuchitapo kanthu, limene limakamba za chionongeko cha anthu amane analipo chigumura chisanafike. Komanso izi zinaonjezera lonjezo lakuti sipadzakhalanso chigumura cha dziko lonse chimene chidzaononge anthu ambiri, komanso lonjezo likukamba zakuti Mulungu adzachulukitsanso anthu (9:1), komanso nyama zimene zidzaperekedwe ngati chakudya (9:2-4), komanso chilango chophedwa kwa wakupha nzake (9:5, 6). Utawaleza unaperekedwa monga chizindikiro kuti Mulungu ndiwokhulupirika molingana ndi pangano limeneli.

Pangano la Nowa linayamba panthawi ya chigumura komanso ndi la muyaya. Monga kukhonza kukhala zigumura zina zimene zikhonza kuononga katundu komanso moyo wa anthu, palibe chigumura chimene chikhonza kukhudza dziko lonse komanso kuononga monga chigumura chachikuru chinachitira. Ufulu wakuti anthu adye nyama unaperekedwa, choncho ife sitiyenera kumasulira ndime zimene zikukamba zakudya masamba okha (Danieli 1) kuti izi zikhale kwa wina aliyense. ndipo chilango chophedwa chilipobe mpakana lero.

4. **Pangano la Abrahamu**
Zinthu zofunikira kudziwa za pangano la Abrahamu zikupezeka mu Genesis 12:1-3, komanso pali zina zoonjezera ndi kufotokozedwa zimene zikambidwabe patsogolo.

Panganoli linaperekedwa kwa Abrahamu ndipo iye anayenera kuchita monga anauzidwira kufikira atakumana ndi kukwaniritsa zimene Mulungu amafuna, ndipo izi zitachitika, pangano linayenera kukhudza anthu ena posatengera kuti iwo apanga chiyani.

Pangano la Abrahamu likuyang'ananso za malonjezano a madalitso kwa munthu, zidzukuru zosawerengeka, malo eni eni, mzinda, dziko labwino, madalitso kamba kochita zinthu limodzi, chitetezo komanso kubwera kwa Mesiya kuchokera ku mbumba yake (Genesis 17:1-8).

Pangano la Abrahamu linayambira kwa Abrahamu. Za pfuko la Mkesiya zinakwaniritsidwa pa ubadwa Yesu Khristu (Agalatiya 3:16). Lonjezo la zinthu zomwe zidzaperekedwe ngati m'dalitso likulumikizana ndi pangano lomwe lakhala likuperekedwa mu nthawi zosiyanasiyana mu mbiri koma zidzakwaniritsidwa bwino lomwe mu ufumu wa zaka chikwi. Pangani iri likupita kwa anthu onse amene kuchokera mu nthawi ya Abrahamu kufikira mu nthawi ya zaka chikwi.

Tanthauzo la ndime ina imene iri yovuta kuimvetsa mu mau a Mulungu, imakhonza kumveka ngati munthu agwiritsa mfundo za Pangano la Abrahamu. Ndime imeneyi ikupezeka mu Mateyu 11:20-24 akuti:

> ***Pomwepo iye anayamba kutonza midziyo, m'mene zinachitidwira zambiri za ntchito za mphamvu, ndipo chifukwa sinatembebuke. Tsoka iwe Korazini, tsoka iwe Betsaida. Chifukwa ngati za mphamvu zimene zinachitidwa mwa inu zikanachitidwa mu Turo ndi Sidoni, akadatembenuka mtima kalekale, mziguduli ndi mphulusa komanso ndinene kwa inu kuti, dzuwa lakuweruza mlandu wawo wa Tulo ndi Sidoni udzachepa ndi wanu. Ndipo iwe kapena awo, udzakedzedwa kodi kufikira kuthambo? Udzatsika kufikira ku dziko la akufa! Chifukwa ngati za mphamvu zimene sidoni uyu ukadakhara kufikira lero komanso ndinena kwa inu kuti dzuwa lakuweruza wake wa Sodomu udzachepa ndi wako!***

Mwachisomo, Israyeli anapatsidwa nthawi yolapa chifukwa cha pangano la Abrahamu. Ngati Israyeli salapa, achimwa, adzalandira chilango chachikuru, komanso dziko lidzaonongedwa ndi kuchotsedwa mu mbiri.

5. **Pangano la Mose**
Pangano la Mose la Chilamulo linaperekedwa kwa Mose pa phiri la Sinai. Pangani limeneri tikhonza kulipeza pa Eksodo 20 ndi ndime zina za Levitiko, Numeri ndi Deutronomo. Pangano iri liri ndi zinthu zoti anthu apange, ndiko kumvera. Iwo amene ali omvera amadalitsidwa, ndipo osamvera amatembeleredwa (Levitiko 26).

Cholinga chenicheni cha pangano la Mose ndikufuna kuonetsera za kufunikira kwa Mpulumutsi (Agalatiya 3:24-25). Pangano iri likuonetsa bwinobwino za lamulo la umunthu lochokera kwa Mulungu. Pangano iri linaperekedwanso kwa Israyeli, kuti akhazikitse ndondomeko ya malamulo a Unsembe wa Alevi komanso Chihema.

Yesu Khristu anabwera kudzakwaniritsa pangano iri posunga bwino Lamulo (Mateyu 5:17). Pangano iri ndi la anthu munthawi ya a Israyeli, komanso likuphatikiza mu nthawi imene Mose amapatsidwa Lamulo (Eksodo 20) kufikira tsiku la Pentekoste pamene mpingo unayamba. Pangano iri lidzaonjezeranso nthawi ya "Mazunzo" imene idzachitike mu zaka zisanu ndi ziwiri utatha mpingo kukwatulidwa.

Ife tiyenera kudziwa kuti pali ndime zambiri mu Chipangano Chakale zimene zimakamba nthawi imene anthu anakhala pa Chilamulo cha Mose. Mwa chisanzo, nyama zina zinalengezedwa kuti "zodetsedwa" ndipo izi sizimayenera kudyedwa (Levitiko 11). Izi sizimatikhudza ife leo lino, chifukwa choti Yesu Khristu ananena mwachindunji kuti zakudya zonse ndi "zoyeretsedwa" (Marko 7:14-18). usunga lamuro (Mateyu 5:17) pangano la Israeli lokha (Eksodo 20) mpakana tsiku la pentekoste pomwe mpingo unayamba.

6. Pangano la Davide

Mulungu anapangana ndi Davide ndipo izi zikupezeka mu 2 Samueli 7:8-9 ndi Masalimo 8. Panganoli ndiloti munthu asapange kanthu, ndipo likunena za ufumu mu nyumba ya Davide komanso lonjezo la "Mwana wamkuru", amene adzalamulire maiko onse kwa muyaya.

Pangano la Davide linayamba kugwira ntchito pamene Davide anali mfumu. Komanso mbali ina yapangano inakwaniritsidwa ndi kubweranso kwa "Mwana wankuru", amene ali Yesu Khristu mwini wake, pa Kubwera kwake koyamba (Luka 1:32). Ndipo zotsaira za izi ndizamuyaya.

Mu nthawi ina, pfuko la Davide linali pansi pa ulamuliro wa mfumu ya zaka zisanu ndi zitatu (8), Yosiya (2 Mafumu 22:1). Mu Yuda okhala mu nthawi imeneyi anali ndi chikhazikitso cha chiyembekezo chomangidwa pa lonjezo la Mulungu. Yesu mwini wake, analandira ulamuliro wonse kumwamba ndi dziko lapansi, chitatha chiukitso chake Mateyu 28:18),pokwaniritsa uneneri wake. Okhulupilira alero angathe kukhala ndi chitonthozo podziwa kuti Yesu Khristu ali pa mpando wa chifumu kumwamba (Ahebri 8:1) chifukwa Iye adzabweranso kuzakhazikitsa mpando wachifumu pa dziko (Mateyu 25:31).

7. Pangano la Palestina

Pangano la Palestina likuonjezera pa za pangano la Abrahamu. Panganoli ndiloti munthu achitepo kanthu komanso ndi limene likupita monga lonjezo kwa Ayuda omwazikana chifukwa chakusamvera kwawo, komabe adzasonkhanitsidwa pamodzi akalapa (Deutronomo 30:1-10).

Pangano iri ndi la m'badwo wa Israyeli ndipo lidzakwaniritsidwa pamene Ayuda adzasonkhanitsidwanso pamene Ambuye adzabwerenso (Mateyu 24:31; Marko 13:27) ndipo dziko lolonjezedwa kwa Abrahamu, kuchokera ku mtsinje wa Firate lidzakhala kuti lakhazikitsidwa (Genesis 15:18). Kuchokera mu nthawi yopereka pangano kupita mtsogolo, omasulira izi ayang'anitsitse kwambiri za kumwazikana kwa a Israyeli kuti kunali kwa nthawi yochepa.

8. Pangano latsopano la Israyeli

Pangano latsopano linaperekedwa ku nyumba ku Israyeli mu Yeremiya 3:31-34 ndipo linabwerezedwanso mu Ahebri 8:8-12. Panganoli linali la mwazi wa Yesu Khristu (Ahebri 9:11-14) ndipo linali loti Ayuda asapange kanthu komabe linali loti iwo alandire moyo wina (Ayuda amene alandiranso moyo watsopano)

Panganoli limanenanso za lonjezo la kukhala kwa Mzimu Woyera kwa munthu wina aliyense komanso kukhala ndi chuma (Yeremiya 32:41; Yesaya 61:8), ndipo lidzakwaniritsidwa mu ufumu wa zaka Chikwi. Ndi chinthu chofunikira kukumbukira kuti pamene tiwerenga mau a Mulungu kuti lonjezo limene linapangidwa ndi Mulungu mu pangano ili linaperekedwa kwa Ayuda okhulupilira okha osati M' yuda aliyense ayi. Ayuda sadzadalitsidwa ndi pangano iri chifukwa cha mtundu wawo monga osankhika.

9. Pangano Latsopano la Mpingo

Pangano la tsopano linapangidwanso ku Mpingo wakuChipangano Chatsopano (Mateyu 26:26-28). Ndipangano loti anthu asapangepo kanthu makamaka Okhulupirira Yesu Khristu, pokhazikika pa mtanda (Hebri 9:11-14) komanso limakumbukilidwa pa mwambo wa m'gonero wa Ambuye- Chiyanjano (1 Akorinto 11:25). Pangano iri linakhazikitsa unsembe wa okhulupirira wa aliyense (Ahebri 9:11) komanso limalonjeza zakukwaniritsidwa mu nthawi ino ndi komanso kwamuyaya. Yesu Khristu anabwera monga Mkhala pakati pa pangano limeneli (Ahebri 9:15).

Panganoli linayamba patsiku la Pentekosite pamene panayambika mpingo (Machitidwe a Atumwi 2) lidzakhala mpaka muyaya. Wphunzira ayenera kukumbukira kuti madalitso ollandiridwa pachipangano ichi ndi amuyaya ndipo wina sangawatenge. Choncho Mpingo wa Okhulupirira a lero, uyenera kuziwa

kuti ndiwotetezeka ndipo ngakhale ungakhale mumavuto otani Ambuye sangaleke ngakhale kuwasiya (Mateyu 28:18-20).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Chaputala 4, Gawo 2F

1. **Kodi ndi mapangano ati amene anali ndi zoti munthu apangepo kanthu?**
   a.
   b.
   c.

2. **Kodi ndi mapangano ati amene anali oti asapange kanthu?**
   a.
   b.
   c.
   d.
   e.
   f.

3. **Werengani ndime zokhudzana ndi pangano lina lirilonse mwa awiri amenewa, ndipo onani ngati mungaonjezere mau ena monga mwa kukamba kwanu mwachidule.**

Gawo 3
Lamulo 3

Funitsitsani Kukhala Anzeru Pofananiza Lemba ndi lemba linzake

Lamulo lachitatu likufunitsitsa nzeru zomwe zikuchokera mu kumvetetsa ndi kugwiritsa ntchito mawu a Mulungu. Tiyenera kuzindikira ndi kuvomereza mwa chikhulupiriro kuti Mulungu sasokoneza (1 Akorinto 14:33), choncho kusamvetsetsa kurikonse kumachokera kwa munthu. Mulungu anapereka miyambi ndi zining'a mu baibulo kuti tiphunzire za nzeru (Miyambo 1:2-6).

Kusamvetsetsa kochuluka pomasulira mau kumabwera chifukwa cholephera kufananiza malemba ndi malemba ena. Munthu omasulira malemba amakhonza kusiya kapena kudumpha ndime zina osazindikira bwino m'mene iye akudziwira ndime ina imene ikhonza kufanana ndi inzake. Ndi chinthu chanzeru kwa iwo amene akufuna kudziwa mau a Mulungu, kuti munthu akhale odziwa za iye mwini komnaso kudzichepetsa kuti adziwe malemba. Iwo amene sanaone bwino kapena kutenga ndime imodzi kapena mau amodzi adzapeza kuti zimakhala zinthu zosiyana kwambiri pokhudzana ndi m'mene munthu angamvetsere mau Malemba.

Pali mfundo 6 zomwe tiyenera kuzidziwa zimene zikugwirizana ndi lamulo iri. Ife tiyenera kuyang'ana za kusiyana pakati pa zimene Mulungu wakhazikitsa pa m'mau ake.ife tiomaona izi poyang'anitsitsa za zimene zimachitika mu nthawi yolembedwa kwa baibulo. Komanso kufananiza ndime pomasulira zimapangitsa munthu kuti afufuze umodzi umene ulipo pa mau a Mulungu, poyang'ananso za zimene ndime zikukamba komanso chisamaliro chimene chikuperekedwa pamene munthu alingalira bwino za ndime zokamba uneneri.

A. Mfundo 9: Onetsetsani za kusiyanitsa

Mfundo imeneyi imatiphunzitsa kuti kuona za kusiyanitsa komwe Mulungu wakukhazikitsa. Mwa njira ina, ife tiyenera kudziwa za kusiyana kwa mau a Baibulo monga, chikhulupiriro ndi ntchito, chipulumutso ndi tchimo, lamulo ndi chisomo komanso ndi zina zambiri. Baibulo likufotokozera kusiyana kwa zinthu zambiri. Koma vuto lathu ndilakuti sitimatha kudziwa za kusiyana kumeneku pamene timasulira mau.

Chitsanzo chodziwa za kusiyana kumeneku chikuoneka pamene tiphunzira za chikhulupiriro ndi ntchit. Mu Aefeso 2:8-10 akuti:

> ***Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo chakuchita mwa chikhulupiliro ndipo ichi sichichokera kwa inu, koma ndi mphatso ya Mulungu, chosachokera ku ntchito, kuti asazadzitamandire munthu aliyense. Pakuti ife ndiye chipango chake, olengedwa mwa Khristu Yesu, kuchita ntchito zabwino, zimene Mulungu anazipangiratu, kuti tikayende m'menemu.***

Ndichachidziwikire kuti chipulumutso chimadzera mu chisomo mwa chikhulupiliro. Koma, kufunikira kwa ntchito sikukuyenera kunyozedwa. Ntchito simapangitsa kuti munthu apulumuke, koma ndizofunikira mu moyo wa chi Khristu.

Chikhulupiliro chilibe mphamvu pa icho chokha, koma chiri ndi mphamvu kamba ka Iye amene timamukhulupirira. Munthu kuti akhale ndi chikhulupiriro mu chikhulupiriro, ndiye kuti iyeyo akudzikhulupirira mwa iye yekha. Tikudziwa kuti tonse tinachimwa, ndipo kuti pa ife tokha tiribe zinthu zoti tingasankhe zinthu zabwino (Aroma 3:23).

Ngati munthu wankuru amayenera kuzudutsa pa malo ena amene pali dzenje koma ndi panyanja, ndipo munthu wina wamupatsa iye chingwe chimene chamangidwa kumthambi, zikhala zinthu zovuta kuti iye akhale ndi chikhulupiriro chifukwa chakuti palibe kudalira kwenikweni pa chinthu chimene iye wapatsidwa chija. Komabe ngati chingwe cholimba chamangidwa ku mthambi waukuru, chikhulupiriro chake chikhalapo chifukwa pali kudalira kwakukuru pa chinthun chimene ali nacho.

Yesu Khristu, amene anasenza machimo athu pa mtanda ndipo anauka kwa akufa, ndiokwanira kukhala monga munthu amene ife tikapo chikhulupiliro chathu

Ntchito zimaimira kuchita china chake chimene chiri chabwino monga mwa chikhalidwe chake, monga kuthandiza osauka (Agalatiya 2:10). Komabe ntchito zabwino sizingathe kutipulumutsa (Tito 3:5). Ntchito zinaikidwa ndi Mulungu kuti zionetse chikhulupiriro chathu mwa Yesu Khristu. Komanso, ife tonse tidzanena kwa Mulungu za m'mene tagwirira ntchito mu dzina la Yesu Khristu ndipo tidzalandira dipo (2 Akorinto 5:10).

Ntchito zichitike kamba ka kuyamikira zimene Ambuye Yesu watichitira. Zisachitike ndi cholinga chofuna kupeza phindu lathu.

Kusiyana kwina kuli kosiyana pakati pa chitetezo cha chipulumutso cha Okhulupirira ndi choonadi cha uchimo m'moyo mwa munthu. Ife tikuuzidwa kuti Ambuye anagwira ntchito yaikuru yakufa ndiyo yopulumutsa, pamene tinari adani ake (Aroma 5:6-10)?

Baibulo limanena kuti okhulupilira akhoza kuchimwa ngakhale ali opulumuka kale:

> ***Tikati kuti tilibe uchimo tizinyenga tokha ndipo mwa iye mulibe choonadi. Ngati tivomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi olungama iye, kuti atikhululukire machimo athu ndi kutisambitsa ndikutichotsera chosalungama chiri chonse. Tikanena kuti sitidachimwa timuyesa iye wonama ndipo mawu ake sakhala mwa ife*** (1 Yohane 1:8-10).

Ndichachidziwikire kuti ndime imeneyi ikukamba za okhulupirira. Ife sitikuyenera kuwerenga kutali mu Chipangano Chatsopano kuti tidziwe za machenjezo kwa Okhulupirira molingana ndi chizolowezi cha uchimo. Funso lomwe liripo ndi lakuti, kodi Okhulupirira amataya chipulumutso chawo pamene achimwa kapena ayi?

Mu buku la Aroma ndi mabuku ena mu Baibulo, chipulumutso chimakhala chamuyaya.paulo anati, ***"chifukwa chake tsopano, iwo akukhala mwa Khristu Yesu alibe kusutsidwa, pakuti chilamuro cha mzimu wa moyo mwa Khristu Yesu chandimasura ku lamuro la uchimo ndi imfa"*** (Aroma 8:1-2). Mpingo wa ku korinto unakhala okhuzidwa ndi machimo ambiri. Paulo anawatchura "akuthupi" (1 Akorinto 3:1-2) koma sananene iwo ngati "osapulumutsidwa". Iye akuwatchura anthu awa ngati "mpingo" umene uli ndi anthu "oyera mtima" (1 Akorinto 1:2).

Zoona zake ndizakuti akhristu akhonza kukhala m'moyo wa uchimo. Ndipo izi ndizachidziwikire kuti chipulumutso chathu sichingataike. ***"Tikakhala opanda chikhulupiliro, iye amakhala okhulupilika"*** (2 Timoteo 2:13).

Moyo wa uchimo wa nkhristu nthawi zonse umakhala ndi zotsatira zake. Ndipo zimapangitsa kuti anthu asalandire dipo; ***"ngati tinkana Iye, Iyeyunso adzatikana ife"*** (2 Timoteo 2:12). Nkhani zokhudza ndime imeneyi molingana ndi zimene zikuchitika panthawi imene ndime imalembedwa zikutsimikiza kuti ife sitidzalamulira pamodzi naye, ngati timukana.

Kuchokera mu zitsanzo ziwiri zimenezi, tikhonza kuyamba kuona kusiyana kumene Mulungu anakukhazikitsa mu Mau ake. Ife tidzakhala moyo wathu wonse kufufuza zimenezi komanso kuyang'anitsitsa pofuna kumvetsa za ubale pakati pa mfundo kaapena mau amene akukambidwa.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Chaputala 4, Gawo 3A

1. **Aefeso 2:8-10, kodi mphatso ya Mulungu ya chipulumutso ndi yotani?**
2. **Tchulani mbali ya munthu pa chipulumutso?**
3. **Munthu akapulumutsidwa? Kodi munthu analengeredweranji?**
4. **Tito 3:5, kodi ntchito za bwino zidzatipulumutsa?**
5. **1 Yohane 1:8, kodi okhulupilira adzakhala mu tchimo?**
6. **1 Yohane 1;9, kodi okhulupilira adzachita chani akachimwa?**
7. **1 Yohane 1:10, kodi tikanena kuti sitinachimwe, kodi timunyenga ndani?**
8. **Ahebri 13:15-16, tchulani ntchito zabwino zomwe zatchulidwa mu ndimezi**
9. **Akolose 3:12-17, tchulani ntchito zomwe zili mu ndondomekoyi**
10. **2 Akorinto 5, Kodi okhulupilira alandira chiyani pa ntchito yabwino**

B. Mfundo 10: Unikirani za zinthu zimene zimachitika pamene ndime zimalembedwa

Mfundoyi yagona pa choonadi choti liwu lililonse, chiganizo, kapena ndime ya mu Baibulo iri ndi uthenga umene ukuoneka pambuyo pake komanso patsogolo pake (kupatulapo mau oyambirira ndi omalizira, chiganizo kapena ndime). Mfundo imeneyi imasamalira kwambiri za malo ake enieni a mau ndi ndime, komanso ubale wa mau ndi ndime. Mulungu akufotokoza bwino lomwe za phunziro limene likupezeka mu mu ndime zimene ziri pafupi – zimene zikukhazikitsa mutu pa ndime zimenezo kapena kudzera mu ndime zimene ziri zofanana ndi mutu omwewo koma mu malo ena mu Baibulo.

Sitiyenera ife kumasulira ndime ndikuiwala za zimene zimachitika pamene ndimeyo imalembedwa ndikupereka tanthauzo labodza. Kugwiritsa nthcito ndime ndikuiwala za zinthu zimene zimachitika pamene ndimezo zimalembedwa ndi njira ya chinyengo yofuna kupereka ndi kutsikimiza za maganizo anu komanso zokhumba zanu. Izi ndi zinthu zosayenera, ndipo ndi njira imodzi younikira tanthauzo pa zinthu zobisika monga takamba kale.

Kumasulira mau potengera za zimene zimachitika panthawi imene mauwo amalembedwa zimatanthauza kuti owerenga amazindikira iye amene amalankhura, kumene uthenga umapita, komanso mutu weniweni wa ndimeyo komanso ndi nthawi iti ndi malo pamene izi zinalembedwa kuti tidziwe bwino za phunziro lake.

Pali mitundu itatu ya kamvesetsedwe ka malembo pa ndime ina iriyonse.

1. **Kumvetsa za malemba molingana ndi zimene zalembedwa pa ndime imene ikuwerengedwa**
   Gawo iri limakamba za ndime zimene ziri mu ziganizo zimene zaperekedwa. Mwa chitsanzo, Agalatiya 5:1, ikutiuza kuti ***"Khristu anatisandutsa mfulu kuti tikhale mfulu, chifukwa chake, musakondweranso ndi goli la ukapolo."*** Mwina tikhonza kukhala ndi chizolowezi chogwiritsa ntchito mau oti "ukapolo" poyerekeza ndi malo komanso nthawi ndi m'mene guru la anthu ena amamvera, chifukwa mau oti "ukapolo" nthawi zambiri amaimira kuti munthu ali pansi pa ulamuliro wa munthu wina, kapena wagulidwa kapena ali m'manja mwa guru lina lake. Mounikira bwino, poyerekeza ndi zimene ndime ikukamba, apa tikuona kuti ukapolo wake ndiwa uzimu. Ndime imeneyi ikukamba za anthu amene anamangidwa ndi miyambo ya Chilamulo (makamaka m'dulidwe) ndipo anthu amenewa siali "afulu" kuti "atumikirane wina ndi mzake mu chikondi" (Agalatiya 5:13).

2. **Kumvetsa za malemba molingana ndi zimene zalembedwa pa ndime motengera ndi zimene ziri m'bukhu lomwelo**
   Gawo limeneli limaona za malemba molingana ndi zimene zalembedwa pa ndime motengera ndi zimene ziri m'bukhu limene likuwerengedwa. Chitsanzo cha ichi chikupezeka pa Mateyu 24:40 ***"pomwepo adzakhala awiri m'munda wina adzatengedwa, wina adzasiyidwa."*** Nkhani imene ikukambidwa apa ikugwirizana ndi nkhani ya "masiku otsiriza". Funso ndilakuti kodi ndi ndani amene adzatengedwe komanso kutsala. Kodi olungama adzatengedwa ndipo oipa adzatsala, monga nkwatulo wa Mpingo; kapena oipa adzatengedwa ndipo olungama adzasiyidwa, panthawi ya Kubweranso Kwachiwiri kwa Khristu kumene kudzakhazikitse ufumu wake wa zaka Chikwi? Gawo lotanthauzira mau iri silimayankha funso ngati limeneli.

   Pa Mateyu 13:49, akupereka yankho. Mu ndime imene ikukamba za "masiku otsiriza" tikuuzidwa kuti ***"padzatero pa chimaliziro cha nthawi cha pansi pano, angelo adzatuluka, nawadzasankhura oipa pakati pa abwino".*** Gawo lotathauzira malemba molingana ndi zimene zalembedwa pa ndime motengera ndi zimene ziri m'bukhu lomwelo layankha funso la iye amene adzatengedwe komanso kutsala. Ndime imeneyi ikukamba za kubweranso kwa Yesu kachiwiri.

   Gawo lomasulira mau limeneli likutidziwitsa za kufunikira kophunzira za ndime ndi ndime kudzera mu bukhu lomwe laperekedwa ndi cholinga chakuti timvetsetse bwino zinthu zonse m'mene zimachitikira. Ngati ophunzira apita mwansanga ku Mateyu 24, yankho ku funso limene liri pa mtundapo sangathe kulipeza. Koma ngati ophunzira atawerenga bukhu lonse kufikira ku Mateyu 24, yanko lingakhale kuti laperekedwa kale.

3. **Kumvetsa za malemba molingana ndi kulumikizana kwa ndime zosiyanasiyana mu Baibulo.**
   Gawo iri limayang'ana za malemba molingana ndi kulumikizana kwawo pa ndime zosiyanasiyana mu Mau a Mulungu**.** Gawo iri limatenga ndime zonse za mu Baibulo zimene ziri ndi mfundo kapena kukamba nkhani ina mu ndime poyerekeza ndi zimene zikukambidwa. Kuphunzira za gawo iri la kumvetsa mau, limaonetsa kuti ndime ina ya mu Baibulo ikhonza kutambasulidwa bwino ndi ndi ndime ina kapena zina zimene ziri mu bukhu lina. Kuphunzira za mau monga "chisomo", "chikhulupiriro" kapena "chikondi" monga mwa chitsanzo, pogwiritsa ntchito bukhu lomwe limakhala ndi ndime zosiyanasiyana, kumathandiza kuti munthu apeze ndime zina zimene zikukamba mau ngati amene akufufuzidwa aja. Bukhu lomwe limakhala ndi ndime zosiyanasiyana, limapereka mau amene

akupezeka mu ndime zina mu Baibulo. Bukhu lamtundu umenewu koma lozama kwambiri liamapereka ndandanda wan dime iriyonse imene iri ndi mau amene inu mukuwafuna. Zambiri zokhudza mabukhu ngati amenewa zikambidwa kutsogoloku.

Mu nthawi zambiri, gawo liemenli limafuna kuti munthu adziwe za mfundo zina ndi zina, monga, kumasulira uneneri kapena kumvetsetsa za "mitundu" ndi "zizindikiro za zinthu zina". Mwa chitsanzo "chophimba cha mukachisi" (Eksodo 26:31-35) chomwe chinalekanitsa malo oyera ndi a oyeretsetsa m'kachisi, chikutanthauza za thupi la Ambuye Yesu Khristu (Ahebri 10:20).

Kutathauzira mau molingana ndi zinthu m'mene zimachitikira ndi chinthu chofunikira kwambiri maka pamene tikufuna kudziwa kuti tikhale "**wolunjika nawo bwino mawu a coonadi"** (2 Timoteo 2:15). Pamene tipanga ziganizo zokhudza **"chiphunzitso cha m'Baibulo"** tiyenera kutsimikizira izi ndi mau a Mulungu kuonetsa kuti Baibulo liri lolumikizana bwino mu zigawo zonse zitatu zothandizira kuti timvetse mau. Ngati chikhulupiriro chathu sichiri chakuti mau onse a Mulungu, akulumikizana ndiye kuti "chiphunzitso" chathu chikhala sicholondora.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Chaputala 4, Gawo 3B

1. **Agalatiya 5:1 ndi Aroma 8:2, kodi tichitenji pa ufulu wa uzimu mwa Khristu.**
2. **Agalatiya 5:13, ufulu umenewu tiugwiritse bwanji ntchito?**
3. **1 Akorinto 10:28-31, kodi tingayankhe bwanji munthu amene akulimbana nafe pankhani ya ufulu?**
4. **1 Akorinto 3:17, Mzimu Woyera amabwera ndi chiyani?**
5. **Yakobo 1:25, lamulo lowona loti tilikakamire ndi liti?**
6. **Yakobo 2:12, kodi tidziyankhura komanso tidzichita motani?**
7. **1 Petro 2:16, tigwire bwanji ntchito mtendere?**
8. **2 Petro 2:1; 17-19, aphunzitsi onyenga amaphunzitsanji?**
9. **Yambani ndi Agalatiya 5:1 (pounikira gawo loyamba lakumvetsa mau), Agalatiya 5:13 (pounikira gawo lachiwiri lomvetsera mau). Ndipo gwiritsani ndime zina zimene zakambidwa pamwambapa (pounikira gawo lachitatu lomvetsera mau) pofuna kuonetsa zizindikiro zina za ufulu.**

C. Mfundo 11: Masulirani Mofafaniza ndime

Mfundo iyi ndiyofunika pomasulira mawu ndipo imaona za kulumikizana kwa ndime zosiyanasiyana mu Mau a Mulungu, ndi kutionetsera kufunikira kofananiza lemba ndi lemba linzake kuti tiunikire bwino za kufanana kwa nkhani imene ikukambidwa, ndi cholinga choti tipeze matanthauzo olondora a mau.

Ndikofunika kufananiza nkhani zimene ziri zofanana ina ndi inzake, monga zokhudza chisomo ndi chifundo, komanso nkhani zimene ziri zosiyana ina ndi inzake, monga Mulungu ndi Satana. Pamene tifananiza za kufanana ndi kusiyana kwa nkhani zimenezi pounikira za kumvetsa malemba molingana ndi kulumikizana kwawo pa ndime zosiyanasiyana mu Mau a Mulungu**,** timaika pamodzi chithunzi chimene chiri choduka pakati – nthawi zina zidutswa zingapo. Maphunziro a za Umulungu amaumbidwa poika zidutswa zimenezi pamodzi.

Osatengera kuti ndi munthu oyamba kumene kumasulira mau (1 Timoteyo 3:16), komanso kwa munthu odziwa bwino kumasulira mau ayenera kukhala osamala pamene ziphunzitso zokhudza Mulungu zikukambidwa, (Miyambo 3:5-6), komanso kuzindikira bwino zinthu zina komanso kudziwa za ndime zoposera 31,000 kuti izi zisataike. Gawo lalikuru la zimene ife tikufuna kumvetsetsa litipangitse ife kuzindikira za zolakwika zina mu Baibulo, choncho tiyenera kukhala osamala kwambiri ndi kudzichepetsa. Tikafananiza lemba ndi linzake timaona kuti mutu wina wokamba za Umulungu ukuoneka mu ndime zina mu Baibulo. Chimodzi mwa chitsanzo ndi nkhani ya "kulungamitsidwa mwa chikhulupiliro" (Genesis 15:6; Aroma 3-4). Pamene tipeza ndime ina yosiyana ndi imeneyi imene ikukamba za "kulungamitsidwa mwa ntchito" monga alemba ku Yakobo 2:14-26, tiyenera kuona ndime zonsezi. Pamene tiika ndime zonse pamodzi, tiyenera kumvetsa mau a "ntchito" monga zofunikira pa dongosoro la Mulungu, monga zomwe

zimabwera chifukwa cha chikhulupiriro, koma osati kuti ndizofunika kutitsogolera ku chipulumutso. Izi zaphunzitsidwa ku Aefeso 2:8-10. Ife "***tinapulumutsidwa mwa chisomo,kudzera mu chikhulupiliro,"*** ndipo "***talengedwa kuti tichite ntchito zabwino."***

Mfundo yomweyo ikutiphunzitsanso kusamala kwambiri pamene tiumba phunziro la za Umulungu, kapena chiphunzitso mu ndime zina kapena kuwerenga motsata ndime ndi kupeza tanthauzo labodza. Mwachitsanzo mu Marko 16:19, mawu a chiGirikiwa kufikira kumapeto kwa ndime imeneyi sakumveka bwino. Anthu ena apanga ziphunzitso kuchokera mu ndime zimenezi, zimene zinawapangitsa kuti akamb za chiphunzitso cha Mulungu chachinyengo.

Chitsanzo china chofananiza ndime ndi ndime zina ndi zikuonekera pa zinthu zimene ziri "zachinsinsi" (kapena kuti zinthu zosadziwika), zimene zikukambidwa kwambiri mu Chipangano Chatsopano. Tikanakhala kuti tikuphunzira "Aefeso 3" ndikufika poona mau oti "chinsinsi" tikanakhonza kuyankha funso loti, "kodi chinsinsi ndi chiyani?" Ndipo yankho liri pa Akolose 1:25-27 pomwe alemba kuti:

> ***amene ndinakhara mtumiki wake monga mwa udindo wa Mulungu umene anandipatsa ine wakuchitira inu wakukwaniritsa mau a Mulungu ndiwo chinsinsicho chinabisika kuyambira pa nthawizo, ndi kuyambira pa m'badwowo, koma anachionetsera tsopano kwa oyera mtima ake, kwa iwo amene Mulungu amafuna kuwazindikilitsa ichi chimene chili chuma cha ulemelero wa chinsinsi pakati pa amitundu, ndiye Khristu mwa inu,chiyembekezo cha ulemelero.***

Chinsinsi chikuzindikiridwa ndi malemba monga chiyanjano chenicheni ndi Mesiya. Chiyanjano chimenechi ndi cha m'badwo watsopano wotchedwa kuti M'badwo wa Mpingo.

Werengani Izi: Chaputala 4, Gawo 3C

1. **Aroma 3:21-28, kodi munthu anganenedwe motani wolungama pamaso pa Mulungu?**
2. **Aefeso 2:8-9, munthu amapulumutsidwa bwanji?**
3. **Yakobo 2:14-26 ndi Aefeso 2:10, wokhulupilira awonetse chiyani?**
4. **Yakobo 2, mlembi akunenanji zachikhulupiliro chopanda ntchito?**
5. **Kodi izi zikutanthauza kuti ngati wokhulupilira saturutsa ntchito, iyeyo sanapulumutsidwe (Tito 3:5)**
6. **Yakobo 2, pokamba za Abrahamu, kodi Abrahamu anali wokhulupilira pamene ankapereka nsembe mwanawake isaki?**
7. **Yakobo 2, ndi munthu uti amene agafunse, "uli ndi chikhulupiliro ndipo ndiri ndi ntchito, ndionetsetu chikhulupiliro chako chopanda ntchitocho, ndipo ine ndikuonetse changa ndi ntchito zake?"**
8. **Ahebri 11:1, chikhulupiliro chingaonedwe kodi?**
9. **Ganizirani za mau onse onena "kupulumutsidwa" mu Yakobo 2:14 ndi "kulungamitsidwa" mu 2:22; 2:24.**

D. Mfundo 12: Funitsitsani kupeza umodzi wa ndime

Mfundo imeneyi imazindikira choonadi ndi kukhulupilika kwa Mulungu, komanso kuti Mulungu siwachisokonezo (1 Akorinto 14:33). Mwa njira ina, palibe zinthu zimene ziri zotsutsana mu Baibulo. Nkhani za Baibulo ndi imodzi, imene inapandigwa ndi kuuziridwa ndi Mulungu Wamoyo, choncho nkhani zina zonse ndi zokhazikika monga zofanana.

Kusutsana pomasulira mau kumachitika chifukwa cha umunthu, osati monga mwa Umulungu. Anthu ambiri amatenga zimene iwo akumva monga kuti ateteze chimene akudziwa pofuna kumva mau a Mulungu, koma Malemba akutichenjeza ife kuchita zimenezo (Yohane 5:37; Miyambo 3:5-6; 2 Akorinto 5:7). Ife sitingathe kumvetsa bwino zinthu zina kapena kwathunthu za Baibulo, kufikira tsiku limene ife tidzakuma ndi Ambuye maso ndi maso (1 Akorinto 13:12). Choncho nkhani ndi yoti ife tonse tiyende mu chikhulupiriro nthawi zonse (Ahebri 11:6; Akolose 2:6) ndipo tikhulupirire Mulungu kuti atitsogolere kumwamba kwathu.

Pamene timvetsa za m'mene ndime zosutsana ziwiri zikulumikizirana ina ndi inzake, tipeza nzeru. Ife tauzidwa pachiyambi cha bukhu la Miyambo kuti pamene timaphunzira zinthu ndi zining'a, timakhala anzeru (Miyambo 1:2-6). Izi zimafuna kuphunzira mwakuya. Mwachitsanzo, monga m'mene takambira tiyenera kuona Yakobo 2 ndi Aroma 3-4 panthawi imodzi, kuti timvetsetsa za chikhulupilira ndi ntchito.

Pamene tiona ndime zimene ziri zokhala pa ubale, tiyenera kuyang'ana za malo ndi nthawi; komanso kuzindikira kuti china chirichonse ngakhale chaching'ono sichinalembedwe, komanso kuti mwina vuto likhonza kukhalapo pamene timasulira mau. Komabe, tiyenera kudziwa kuti palibe mau amene amatsutsana ndi anzake m'mau a Mulungu. Ife tiyeneranso kuvomereza kuti mau a Mulungu, pafupipafupi za mfundo yomweyo koma mu njira yosiyana ndi cholinga choti mfundo yofunikira ilandiridwe mwakuya. Mwa chitsanzo Aroma 3:23 amati, "pakuti onse anachimwa" chimodzimodzinso bukhu la Levitiko likutilamula ife kuti kubweretsa nsembe yauchimo. Ndime zonse zikukamba zimodzi.

Chimenenso chikukhala chomveka bwino, kuchokera pa kuwerenga kwathu kwa mau a Mulungu, ndi kwakuti Mulungu analondolera za kalembedwe ka mau ndi dongosolo lake.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Chaputala 4, Gawo 3D

1. **Kodi ndondomeko imene yatsatidwa mu gawo la m'mbuyo (3C) ikuonetsa mfundo iyi?**

2. **Aroma 3:21-28; 5:1-2; 8-10; Yohane 10:27-29. Tchulani mfundo yeniyeni ya chipulumutso?**

3. **1 Akorinto 6:9-10, kodi ndimezi zikutiphunzitsa chiyani?**

4. **Kodi izi zikuoneka kuti zikutsutsana?**

5. **1 Akorinto 3:10-15, munthu apange chiyani kuti akonze za chiyanjano?**

6. **Yakobo 1:12, munthu achitenji kuti alandire korona wa moyo?**

7. **1 Petro 5:1-4, munthu atani kuti alandire Korona wa Ulemelero?**

8. **2 Timoteyo 4:7-9, munthu atani kuti alandire Korona wa Choonadi?**

E. Mfundo 13: Ganizirani Kusintha kwa Nthawi

Kusintha kwa zinthu ndi nthawi mu mbiri kunakhazikitsidwa ndi Mulungu, ndipo Iye anapereka udindo wosiyanasiyana kwa anthu ake. Pali zigawo mu mbiri zimene zikuonetsedwa komanso kuperekedwa kwa udindo kwa anthu. Tikumva mu Ahebri 7:12 kuti, ***"pamene unsembe usintha, chilamuro chiyenera kusintha."*** Ndime imeneyi imatiphunzitsa kuti Mulungu anakhazikitsa maudindo osiyanasiyana mu nthawi zosiyanasiyana mu mbiri.

Pali kusintha kunai kuyambira pa kuchimwa kwa Adamu:

1. **Nthawi ya a Mitundu kuchokera pa kuchimwa kwa Adamu kufikira kuchoka kwa ana Israyeli ku Aigupto**
   Izi zalembedwa kuchokera ku Genesis ndi Yobu. Ndipo izi zikufikira munthawi ya 3900 B.C.–1445 B.C.

2. **Nthawi ya a Israyeli pamene anachoka ku ukapolo ku Aigputo kufikira Tsiku la Pentekosite**
   Izi zikupezeka mu mabuku a Chipangano Chakale kupatura mu buku la Genesis ndi Yobu. Ndipo zikupezekanso mu bukhu anai a uthenga wabwino ndi Machitidwe Atumwi ku Chipangano Chatsopano. Pali ndime zina mu Chipangano Chakale zimene zimanena za zaka chikwi. Ndipo zitsanzo ziwiri ndi Yesaya 61-66 ndi Ezekieli 40-48.

   Zaka zake za nyengo imeneyi ndi 1445 B.C. mpaka A.D. 33. ndipo nyengo imeneyi imayang'ananso za "m'kwatulo wa mpingo mpaka kudzanso kwa Khristu (Danieli 9:24-27). Iyi ndi nthawi ya chisautso chachikulu cha chi Khristu kapena kuti Sabata ya 70 ku Danieli.

3. **Nthawi ya Mpingo Kuchokera Tsiku la Pentekosite Mpaka Mkwatulo**
   (Chisautso chachikulu chomwe ndi zaka zisanu ndi ziwiri zomaliza pa zaka za Israyeli kuchokera pa mkwatulo mpaka kudzanso kwa Yesu.)

Zaka zimenezi zili mu Machitidwe 2-28, mu Makalata ndi Chibvumbulutso 2-30. Chisautso chachikulu chidzamaliza zaka za Israyeli zimene zikupezeka mu Chibvumbulutso 4-19.

Zaka zi zinayamba mu 33Yesu atafa (AD) ndipo sizinathe mpaka m'kwatulo wa mpingo udzachitike.

4. Nthawi ya Zaka Chikwi Kuchokera paKubwera kwa Yesu Mpaka Nthawi ya Mpando Woyera wa Chiweruzo

Mbiri imeneyi zinalembedwa mu Chivumbulutso 20 komanso mu malemba ena mu chipangano Chakale ndi Chatsopano.

Kusinthako kuyenera kumvesetsedwa bwino, makamaka potengera ndi unsembe wosiyanasiyana umene Mulungu waupereka kwa anthu. Mwachitsanzo Israyeli asanakhale pfuko isanafike nthawi yochoka mu ukaplolo ku Aigupto,anthu anali mu nthawi yogawidwa "Nyengo ya a mitundu". Unsembe wa nthawi imenyi umachitika ndi akuluakulu amu "banja la ansembe". Ndipo izi zinachitidwa ndi Nowa (Genesis 8:20), Abrahamu (Genesis 22:2) ndi Yobu (1:5). Malamuro amene iwo anayenera kutsatidwa anali iwo amene ***"analembedwa mu mitima yawo"*** (Aroma 2:15).

Mwachidule itatha nyengo yotuluka ya Ayuda kuchokera ku Aiguputo, ndipo pfuko la Levi linaitanidwa ndi Mulungu ku unsembe wina, "unsembe wa chiLevi". Unsembe umenewu unali ndi maziko ake kuchokera ku m'badwo ndi ana onse ochokera kudzera kwa Aroni, wapfuko la Levi. Unsembe wachiLevi umenewu unkachita ntchito yawo mu poyambirira mu Chihema kenako mu Kachisi. Ansembe a nthawi imeneyo ankapereka nsembe yopsereza kwa Mulungu ndipo izi zinatsogolera anthu pakupembeza ndi kupereka Mau a Mulungu, koma pogwiritsa ntchito njira zeneizeni zimene Mulungu anamupatsa Mose. Malamulo omwe anayenera kutsatira analembedwa mu Eksodo, Levitiko, Numeri ndi Deutronomo. Monga mfundo yoonjezera, ndi zinthu zochititsa chidwi komanso kumvetsa chisoni kuti njira zimene zaonongedwa munthawi imene Yesu anabadwa, kuti mwambo umenewu unakhala wofunikira kwambiri kusiyana ndi zimene mwambo umenewu umatanthauza.

Pemene Yesu anamwalira ndikuuka kwake kwa akufa, pa tsiku la Pentekosite, Mulungu anayamba nthawi ina yatsopano yogawa udindo kwa anthu. Ndipo izi zimatchulidwa kuti "zaka za Mpingo" kapena "kusintha kwa zinthu mu Mpingo". Mu dongosolo losintha zinthu izi, iwo onse amene anakhulupirira Yesu Khristu, anakhala ansembe a Mulungu (1 Petro 2:5, 9). Ndipo "Okhulupirira-Ansembe" atsopanowa sayenera kupereka nsembe yopsereza koma m'malo mwake anali ***"kupereka matupi awo monga nsembe yamoyo ndi yoyera, yovomerezeka kwa Mulungu, yomwe ndi ntchito ya mapembezo"*** (Aroma 12:1). Mu nthawi imeneyi, yakusintha kwa zaka za mpingo, machitidwe a unsembe anasintha. Komabe, ntchito za uzimu za unsembe wina ndi wina sizinasinthe. Onse anali kupereka nsembe, komanso kutsogolera matamando ndi kupereka Mau a Mulungu. Nyengo yosintha imaonetsedwa mu njira zosiyanasiyana zimene Mulungu amazigwiritsa kukwaniritsa cholinga chake. Nthawi yosintha ya mpingo imeneyi tiyenera kuyendera "Lamuro la ufulu" (Yakobo 1:25; 2:12) pounikiranso "nyengo ndi zochitika za chikondi" (Aroma 13:8-10; Agalatiya 5:14; Yakobo 2:8).

Nyengo ya zaka chikwi kapena nyengo yakusintha idzakahala ndi unsembe wotsogozedwa ndi anthu akum'badwo wa Zadoke mu pfuko la Levi (Ezekieli 40:46; 43:19; 44:15; 48:11). Malamulo adzakhazikika pa "pangano latsopano la Israyeli" (Yeremiya 31:31-33; Ahebri 8:8-10), amene anakhazikitsidwa ndi Ambuye Yesu yekhayo popeza iye ***"amalamulira mafuko ndi ndodo ya mkuwa"*** (Chivumbulutso 12:5).

Kumasulira molingana ndi kusintha kwa nthawi, kumazindikira kusintha kwa zinthu m'mene zimakhalira, komanso zimenezin ziri ndi maziko ake mu zinthu zauzimu kusiyana ndi zathupi. Mwachitsanzo, mu nthawi yathu ino, ife sitiyenera kupereka nsembe za nyama, mpingo umatenga kale mbali pa M'gonero wa Ambuye monga chkumbukiro ku nsembe yeniyeni ya Ambuye Wathu Yesu Khristu (Ahebri 10:10), monga nsembe yamatamando (1 Akorinto 11:23-34). Pa nthawi ya Zaka chikwi, kuperekedwa kwa nyama monga nsembe kudzakhazikitsidwanso monga chikumbukiro chokumbukira ntchito imene Yesu Khristu anaimaliza pa mtanda (Ezekieli 43:18-27).

Zigawo za mbiri zimatengedwa kuchokera ku njira yomasulira mau ndipo sinjira yokhazikika. Pali njira zingapo zimene anthu akhonza kuganizira za nthawi yeniyeni pa kusinthasintha kwa nyengo. Komabe izi sizikupangitsa kuti mfundo yokamba za kusintha kwa nthawi kuti ikhale yopanda pake ndi m'mene Mulungu anaperekera udindo kwa anthu mu nyengo zosiyanasiyana mu mbiri.
Pali njira ina yamakono yoona za "kusintha kwa nthawi mwamakono", ndipo njira imeneyi imaika magawo ena onse ang'onoangono pamodzi pounikira zimene zikuchitika mu mbiri. Tiyenera kudziwa kuti dongosolo iri limatsimikiziridwa ndi ndime zochepa za m'Baibulo. Izi zingapangitse kuti anthu apange zinthu monga mwa zokhumba zawo komanso kuononga kumasulira koona. Kusamasuka kwenikweni kwa mfundo imeneyi ikhoza kutipangitsa ife kuti tikhale otsata chilamulo komanso

kulephera kupeza mwayi oti titumikire m'moyo wa Chikhristu. Mwa chitsanzo, kulephera kupeza tanthauzo la Mpingo pa Chiphunzitso cha Paphiri, chifukwa chakuti Yesu analankhura mfundo zina mu Nthawi ya Israyeli, zikhonza kupangitsa kuti anthu ataye zonse zimene tikuuzidwa ndi Paulo mu 1 Timoteo 6:3, "chiphunzitso choona" ndi "mau oona" ndi a Ambuye wathu Yesu Khristu.
Zimene ife tiyenera kuyang'ana ndi kukamira ndi mfundo zimene ziripo pa maphunziro a kusintha mu mbiri. Njira zosiyanasiyana za unsembe zasintha mu Baibulo, koma mfundo zake zimene zimakhazikikapo sizinasinthe. Ansembe onse a munthawi ina iriyonse alamulidwa kuti abweretse nsembe kwa Ambuye kommanso kuphunzitsa Mau a Mulungu.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Chaputala 4, Gawo 3E

1. **Werengani Ahebri 7:12 unsembe ukasintha, chimasinthanso ndi nchiyani?**

2. **Werengani Genesis 8:20; Yobu 1:5, izi ndi zintsanzo za unsembe mu nthawi ya Amitundu. Ndipo zikutchulidwa kuti "Banja la Unsembe". Kodi ndi ndani ali mwini wakupereka nsembe?**

3. **Werengani Aroma 2:5, mu nthawi ya Amitundu, ndi lamulo liti limene linkatsatilidwa?**

4. **Werengani Eksodo 28:1, ichi ndi chitsanzo cha unsembe nthawi ya a Israyeli. Kodi ndani ali ulamuliro wopereka nsembe?**

5. **Werengani Deuteronomo 4:44-46, kodi ndi lamulo liti limene Israyeli ayenera kutsatira?**

6. **Werengani 1 Petro1:1-2 ndi 2:5, 9, kodi a nsembe mu nyengo ya mpingo ndi ndani?**

7. **Werengani Aroma 13:8-10, Yakobo 2:8, ndi lamulo liti limene a nsembe a Mpingo ayenera kutsatira?**

8. **Werengani Ezekieli 40:46; 43:19; 44:15; 48:11, ndani ali a nsembe mu nyengo ya zaka chikwi?**

9. **Werengani Ahebri 8:8-10, ndi lamuli liti limene likulamura zaka zino?**

10. **Ansembe a Levi ankathira nsembe zopsereza, ansembe a chifumu ankadzipereka okha nsembe, kodi zikusiyana bwanji pamenepa?**

F. Mfundo 14: Chenjerani ndi uneneri

Mfundo iyi imazindikira kuti Baibulo limalosera zamtsogolo. Komanso Baibulo limatiuza kuti ulosi weniweni oona umabwera kuchokera kwa anthu amene anatsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, ndipo "palibe uneneri wa mau umene umadzifotokoza za iwo eni" (2 Petro 1:19-21). Pakhala pali kuyesera kosiyanasiyana kwa anthu pomasulira uneneri, ndipo ndizomvetsa chisoni kuti, anthu ambiri ndi a chinyengo. Ndi chinthu chachidziwikire kuti magulu a anthu ena achipembedzo, amatha kugwiritsa ntchito njira zapaderadera pomasulira uneneri, monga njira yokopera anthu ena. Kumbukirani kuti monga okhulupirira mwa Yesu Khristu, ife tonse ndife ansembe. Chenjerani ndi anthu amene ali ndi matanthauzidwe atsopano komanso achilendo; chenjerani ndi anthu amene akufuna kuti inu mukhulupirire mamasulidwe awo atsopano ndi apaderadera ndicholinga chakuti mulowe mu guru lawo.

Omasulira uneneri amaika zinthu zonse pamodzi poona chithunzi chachikuru chimene chadulidwa mu zigawo zosiyanasiyana zambiri (pali ndime ndithu zokwana zikwi khumi za uneneri). Pamene chithunzithunzi chakwanira, ife tiyenera kuona nkhope ya Khristu, amene ali oti timuyang'ane mu mbir yonse, yakale, yatsopano komanso yamtsogolo. Chinthunzi chimene chikuoneka chiyenera kugwirizana ndi mfundo zonse zodziwika ndipo tiyenera kutenga zidutswa zonse ngati umboni. Sichinthu chabwino kutenga zinthu zimene siziri zogwirizana ndi chithunzi chimene tikhonza kuona.

Kuphunzira za kumasulira uneneri ikhonza kukhala phunziro lapaderadera, chifukwa chakuti theka la theka la malemba ndi mabuku a uneneri. Ndi cholinga cha phunziro iri, pali ndondomeko zitatu zotitsogolera pomasulira uneneri.

1. **Unikirani Ngati Mneneri akupereka Tanthauzo**
   Poyamba, onani ngati m'neneri akupereka tantahauzo lake monga Yesu anchitira mu Yohane 2:19-21, zokhudza Kachisi. Ndime ikuti;

Yesu anayanhkha iwo nati, phwasulani kachisi uyu, ndipo ine ndidzamanga pakatha masiku atatu ndipo ayuda anapsa mtima nati makolo athu anatenga zaka makumi anayi ndi mphamvu zisanu ndi chimodzi kumanga kachisiyu, ndipo uyu akuti adzamanga "masiku atatu."

Uneneri ngati uwu ndiosavuta kutanthauzira. Komanso zindikirani kuti Mulungu nayenso akhonza kukolora pa zinthu zake pakupita kwa nthawi osanena kanthu. Komanso akhonza kukolora pakupita kwa nthawi mu ndime yomweyo, monga m'mene zikufananirana pa Luka 4:18-21 ndi Yesaya 61:1-2, pamene Yesu anaigwiritsa ntchito ndime imeneyi komanso kumasulira.

2. **Onani Ngati Ulosi Uli ndi Mbiri Yomwe Yakwaniritsidwa**
   Choyamba tiyenera kufufuza ngati nkhani ya mu malemba yaulura uneneri wina kapena ngati unakwaniritsidwa. Izi zimapangitsa ife kuti ndi uneneri uti umene sunakwaniritsidwe, choncho mwina mtsogolo. Chitsanzo ndi chigumura cha Nowa chimene chinalongosoledwa zaka 120 chisanachitike (Genesis 6:3). Malemba atiuza kuti izi zinakwanilitsidwa (Genesis 7-8).

   Malembo amanenanso kuti Ambuye adzasonkhanitsa Israyeli (Zekaliya 9:14; Mateyu 24:31). Uneneri umeneu sunakwaniritsidwe. Izi tikuzidziwa kuchokera mu malemba komanso mu mbiri.

   Tiyenera kuyang'ana mabuku ena monga a mu mbiri, kuti tidziwe kuti ngati uneneri unakwaniritsidwa. Kumbukirani kuti mbiri ya dziko siinauziridwe ndi Mulungu ndipo siingathe kugwirizana ndi mau a Mulungu nthawi zina, koma ophunzira Baibulo nthawi zonse ayenera kuvomereza kuti Mau a Mulungu ndi oona.

3. **Zindikirani Chiyankhuro cha Ulosi**
   Mu uneneri tiyenera kuganizira mawu komanso chiyankhulo chomwe chikugwiritsidwa ntchito monga monga mau oimirira "mwana wankhosa wa Mulungu" "mkango wa pfuko la a yuda" (Chibvumbulutso 5), zifanifani monga chilombo (Chivumbulutso 13) ndi zinthu monga zina "Likasa" (limene likupezeka mu Eksodo 25-40). Ndi chinthu chachidziwikire kuti pano, choyambirira tiyenera kuyang'ana matanthauzidwe a uneneri, molingana ndi m'mene akulankhulira mu uneneriwo.

   Kumbukirani kuti zimene anthu akungoganiza sikutanthauzira mau. Zimene anthu akungoganiza zimabwera pamene anthu aganiza za zimene zikulankhulidwa mu uneneri. Ndi zinthu zosavuta kuti anthu atenge zinthu zongoganiza ndikuuziika mu "chiphunzitso". Tiyenera kudziwa kuti ziyankhuro mu maulosi ena sizimamveka bwino mpaka nyengo yake yoikika (Danieli 12:4; 8-10).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Chaputala 4, Gawo 3F

1. **Werengani 2 Petro 1:19, Chifukwa chakuti Yesu anabadwa, kumwalira ndi kuukanso pokwaniritsa uneneri, tinganene chani za mau a uneneri wake?**

2. **Werengani 2 Petro 1:20, kodi chofunika ndi chiyani pa ulosi oona?**

3. **Werengani 2 Petro 1:21, koodi ndi ulosi owona unaneneledwa kwa ndani ndipo umapita kwa ndani?**

4. **Werengani Luka 4:18-21; Yesaya 61:1-2, Yesu ananena chiyani pa zomwe zimachitika pa nthawi imeneyo?**

5. **Werengani Genesis 6-8, ulosi ukunenedwa mu 6:3, kodi unakwaniritsidwa?**

6. **Werengani Yesaya 7:14 ndi Mateyu 1:18-25, ulosi umenewu unakwaniritsidwa kodi?**

7. **Werengani Yohane 14:1-3, ulosi unakwaniritsidwa kodi?**

8. **Werengani 1 Atesalonika 4:16-17, kodi ulosi umenewu unakwaniritsidwa?**

9. **Werengani Zekaliya 14:1-8, kodi ulosi unakwaniritsidwa kodi?**

10. **Funitsitsani kuonetsa kusiyana kwa zochitika mu 1 Atesalonika 4:16-17 ndi Zekariya 14:1-8.**

11. **Werengani Chibvumbulutso 5:4-6, ndipo tchulani mau osiyanasiyana olongosora za Yesu Khristu.**

Gawo 4
Lamulo 4

Funitsitsani Kukhala M'moyo wa Khristu Pogwiritsa ntchito bwino Mau a Mulungu

Lamulo limeneli likubwera mwachindunji kuchokera pa mau a Yesu Khristu amene akupezeka mu Yohane 7:17 amene akuti, "ngati tidziwadi mau a Mulungu" ndipo tiyenera kufunisitsa kuwachita mauwo". Mfundo imeneyi imaonetsa kufunikira kwa nzeru zimene anthu amakhala nazo pamene afuna kuphunzira Mau a Mulungu. Tiyenera kusiya maganizo athu ndi zina zonse zimene ziri zanthu ndikulora kuunikiridwa ndi Mzimu Woyera (1 Akorinto 2:14). Pogwiritsa ntchito mfundo imeneyi, kumakhudz za moyo wanthu, mwa chitsanzo, kuunguza za chiyero m'malingaliro athu (2 Akorinto 13:5).

Ndi zinthu zosavuta kuti ife tikhale oona pa nkhani za ife eni kapena maganizo osafunikira kenako ndikuyamba kuyang'ana "chitsimikizo" cha Baibulo pa nkhanizo. Komabe pogwiritsa ntchito njira imeneyo, tikhonza "kupeza umboni" pa chinachirichonse, chifukwa zimatipanga ife kukhala osadziwa za ndime zimene zikhonza kutitsogolera ku zinthu zina, kapenanso ndime zimene zikhonza kutiuza ife zinthu zoti tikhonza kuziunikira bwino. Mwa chitsanzo munthu angathe kungoona machitidwe a Davide pa Betiseba, mkazi wa m'modzi wa ankhondo ake (2 Samueli 11). Anthu ena akhonza kugwiritsa ntchito ndime pofuna kutsimikiza kuti ndi chinthu chotheka kuti munthu amene ali ndi udindo akhonza kupha komanso kuchita chigololo. Munthu ayenera kuwerenga mutu otsatira kuti afananize bwino ndi "Malamulo Khumi" Eksodo 20:1-17, ndi kuona kuti kupha ndi chigololo ndi zinthu zosavomerezeka pamaso pa Mulungu. Koma Davide anapitilirabe kukhala mfumu mwa chisomo cha Mulungu chimene anachionetsa Davide atalapa (Masalmo 51).

A. Mfundo 15: Kugwiritsa Bwino Ntchito malemba zikutengera ndi Matanthauzidwe olondora

Kugwiritsa Bwino Ntchito malemba zikutengera ndi Matanthauzidwe olondora. Pakhonza kukhala njira zambiri zogwritsa ntchito Mau a Mulungu, koma pali njira yolondira imodzi yomasulira ndime. Mwa chitsanzo 1 Timoteo 3:1-4, akunena za, "oyang'anira" mu mpingo. Kumasulira uku kukuonetsa zomuyenereza kuti akhale pa mpandowu. Kugwiritsa ntchito kwa ndimeyi kukutanthauza kuti "oyang'anira" sakuyenera kukhala wotembenuka mtima kumene" koma kuti zomuyenereza zimene zakambidwa zikuonetsa kuti akhale okhwima ndipo ichi chikhale cholinga kwa wina aliyense amene ali mu mpingo, makamaka atsogoleri.

Kugwiritsa ntchito koyenera kwa mau a Mulungu, zikutanthauza kuti munthu wagwiritsa ntchito njira ndi malamulo amene ife takamba mwanzeru ndi moona mtima. Ndiye kuti munthu wapeza nzeru kwa Mulungundi cholinga choti pakhale ubale wabwino ndi Mulungu umene ukukhazikika pa chikhulupiriro komanso chisomo. Ndiye kuti munthu ayenera kutenga mphamvu kwa Yesu Khristu kudzera pa kutsogoleredwa ndi Mzimu Woyera.

Ndime zomveka bwino zakhala chitsogozo cha pa moyo wamunthu, ndipo ophunzira ayenera kudziwa za umodzi wa Mau a Mulungu (potengera ndi m'mene iye akudziwira Mau a Mulungu), ndi cholinga choti tikhale m'moyo wolungama koma osati wachilamulo komanso kugawana za m'mene Khristu aliri pa moyo wanthu.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Chaputala 4, Gawo 4A

1. **Werengani 1 Timoteo 3:1-7, ndipo tchurani zomuyenereza woyang'anira mpingo.**

2. **Onse ofuna ubusa, aziyese okha pazowayenereza zonsezi pamene afuna kukhala abusa.**

B. Masitepe Asanu ogwiritsa ntchito Mau

1. Pempherani kuti mumvetsetse bwino, ndi kutenganso nkhani zina ndi kugwiritsa ntchito bwino mfundo za uzimu molingana ndi (Yakobo 1:5).

2. Funitsitsani kumvetsa molondora ndikuwerenga bwino ndime imene yaperekedwa. Izi zimatengera kuti munthu aphunzire ubae wa mau amene ali mu ziganizo, ndi ziganizo zimene ziri mu ziganizo zingapo, komanso zimene zikuoneka mu ma chaputala, ndi machaputala amene akuoneka mu mabuku (2 Timoteo 2:15).
3. Ganizirani mfundo za yauzimu yomwe imadza kuchokera pamene mwatanthauzira ndime. Mfundo ya uzimu imafikira ku nthawi komanso ku zikhalidwe zonse. Mwa chitsanzo, nkhani ya chigolo (munthu

kugona ndi munthu wina kunja kwa banja) ndi tchimo kuchikhalidwe komanso mu nthawi zonse. Mfundo ya uzimu ndiyakuti danani nacho chigololo (Aroma 13:8-10).

4. Moona mtima unguzani moyo ngati simunatsutsane ndi mfundo zina za malembo, komanso dziperekeni nokha kwa Mulungu povomereza zoipa zimene munachita ndi kulapa. Izi zimatengeranso kuvomereza kwenikweni koona pa zimene mwalakwitsa kwa Ambuye (1 Yohane 1:9) komanso kudziyeretsa nokha pa chikhulupiriro chanu (Akolose 2:6). Wophunzira awerenge Masalmo 51 ndikupeza zimene Davide anachita polapa uchimo womwe anachita ndi Betiseba (2 Akorinto 13:5).

5. Yendani mu chisomo ndi chikhulupiliro. Mtumwi Paulo akutiuza kuti, ***"popeza tsono munalandira Yesu Khristu amuye, yendani mwa iye"*** (Akolose 2:6). Tinalandira Iye mwachisomo kudzera mu chikhulupiliro (Aefeso 2:8-9), ndipo ife tiyenera kuchita ntchito zogwirizana ndi chisomo chimene tinalandira (Aefeso 2:10).

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Chaputala 4, Gawo 4B

1. **Werengani Yakobo 1:5, kodi tikumva zotani zoti tipempherere?**

2. **Werengani 2 Timoteyo 2:15, kodi chofunika ndi chiyani kuti timvetse komanso kugwiritsa ntchito mau a Mulungu.**

3. **Potengera ndi 1 Timoteo 3:1-7, tchulani mfundo zenizeni za uzimu?**

4. **Chifukwa choti makhalidwe awa ali oyenera kwa oyang'anira mpingo, kodi izi sizoyenera kwa wokhulupilira wina aliyense?**

5. **Unikirani moyo wanu molingana ndi mfundozi?**

6. **Ngati pali zina zoti mulape kwa Ambuye ngati uchimo? Ngati ndi choncho, lapani ndithu.**

7. **Kodi pali Ngati pali zina zoti mukonze mu mayendedwe anu a chikhulupiliro, ngati ndi choncho, muli okonzeka?**

C. Zolepheretsa Zisanu Ndi Chimodzi pomasulira Mawu

Njira zisanu ndi zitatu zimenezi ndizosavuta monga m'mene zalembedwera, koma ziyenera kutengedwa ndi wophunzira Mau a Mulungu, chifukwa pali mulingo umene munthu aliyense akhonza kulephera pomasulira mau. Ndi chinthu chofunikira kwambiri kuti titenge ndime imene iri yomveka kuti ititsogolere. Tiyeni tione Miyambo 3:5-6 imene ikunena kuti, "***khulupirira Yehova ndi mtima wako wonse, osacirikiza pa luntha lako, Umlemekeze m'nira zako zonse, ndipo Iye adzaongola mayendedwe ako***".

1. Zathupi

Cholepheretsa choyamba pomasulira Mau ndi nkhani za kuthupi. Nkhani ya kunthupi imaonetsa za moyo opitilira wauchimo zimene nthawi ina zimatchulira kuti "zathupi." 1 Akorinto 3:3. Izi zikusonyeza kuti munthu okhulupirira wasankha kuchita uchimo kudzera mu "ntchito za thupi" osati za kutsogoleredwa ndi Mzimu Woyera ndikuona chipatso chake (Agalatiya 5:19-23). Uwu ndi moyo wa munthu amene sanalape machimo ake (1 Yohane 1:9) ndi kulephera kulapa (2 Akorinto 12:21).

Ngati wina aphunzira Mau a Mulungu ndikuchitanso ntchito za kuthupi, monga dama, codetsa, kukhumba, zonyasa, kupembedza mafano, nyanga, madano, ndeu, kaduka, zopsa mtima, zotetana, magawano, mipatuko, njiru, kuledzera, mcezo, ndi zina zotere (Agalatiya 5:19-21)- ndiye kuti kumasulira kwake kukhala kolakwika. Mwa chitsanzo, mphunzitsi amene amene akuchita chigololo akhonza kukhala ndi mtima oononga ndime zimene zikukamba za mutu ngati omwewo.

Chifukwa chakuti choonadi chavumbulutsidwa ndi Mzimu Woyera (Yohane 16:13) ndipo ntchito za "thupi" zasankhidwa kutsogolera moyo osiyana ndi kutsogoleredwa ndi Mzimu Woyera (ngakhale itakhala nthawi yochepa), kuti ngakhale munthu "wakuthupi" adzakhonza kutenga choonadi chimene chaonongeka, chifukwa chakuti iwo siali "munthu wokweza zinthu za uzimu" molingana ndi Mau a Mulungu.

Munthu "wakuthupi" akufana ndi munthu "wachikhalidwe" 1 Akorinto 2:14, koma ndi zosiyanako pang'ono. Munthu "wachikhalidwe" akuyenerezedwa nd munthu osakhulupirira amene ***"salandira za mzimu wa Mulungu pakuti aziyesa zopusa ndipo sakhoza kuzizindikira chifukwa ziyetsedwa***

mwa uzimu." "Munthu wakuthupi" alibe mwayi wolumikizana ndi Mzimu, pamene anthu "akuthupi/aumunthu" ndi okhulupirira amene siali pa chiyanjano ndi Mzimu. Komanso iye sangathe kumvetsa Mau a Mulungu.

2. Zachabe

Zachabe zikutanthauza kufunitsitsa kwa munthu kuti akhale otchuka kapena kufuna kupezeka pakati pa anthu komanso kufuna kuyamikiridwa. Zachabe zikhonza kutanthauzanso kupangitsa anthu kumasulira zinthu zimene molakwika. Ife tachenjezedwa mu Miyambo 16:18 kuti ***"Kunyada kutitsogolera ku chionongeko, mtima odzikudza utisogolera kukupunthwa."*** Awa ndi malangizo abwino kwa munthu amene akumasulira mau.

Pamene ziri za chidziwikire kuti tiyenera kuphunzira mwa tcheru Mau a Mulungu, ndi zoonanso kuti tiyenera "kuwatenga Mau molondora" (2 Timoteo 2:15). Kuphunzira kwathu Mau a Mulungu kuyenera kukhala kotsogozedwa ndi chikondi cha pa Ambuye komanso anthu ena, akuti, Marko 12:29-31, osati chokhumba chathu kuti tidziwike ndi malingaliro athu a nzeru. Kuphunzira chinthu china "chatsopano" zimene zimakuza chidziwitso chathu cha umunthu ndi zinthu zofunikira kwambiri pa kukula kwathu kwa moyo wa uzimu, komanso ngati tifunitsitsa kuyang'ana Mau a Mulungu, kuti tiphunzire zinthu zina zatsopano ndi cholinga anthu adziwe kuti ife timadziwa Mau a Mulungu ndiye kuti tikuchita ndi cholinga cholakwikwa komanso tikufuna kuti anthu atione.

3. Tsankho

Chinthu china chimene chimalepheretsa kumasulira Mau a Mulungu molondora ndi tsankho. Mau oti tsankho ndi amene amatanthauza kuchita zinthu zimene zokomera iwe mwini, ndipo izi zimapangitsa kuti ndime zionongeke pamene zimasulidwa chifukwa zimaonedwa molakwikwa. "Sindikufuna kuti chinthu chioneke motere." Ngati maonedwe amenewo ali okhazikika akonza kuononga mbali zina za Mau a Mulungu.

Ndi zomvetsa chisoni kuti anthu agwiritsa ntchito maganizo awo ndi cholinga chofuna kuti alungamitse Mau a Mulungu, choncho maonetdwe amenewa osala zinthu zina ndi oipa komanso Baibulo limatsutsa zimenezi. Agalatiya 3:27-29 akuti,

> ***Pakuti nonse amene munabatizidwa kwa Khristu munavala Khristu, muno mulibe myuda kapena mherene kapena kapolo, kapena mfulu, kapena mkazi, kapena mamuna. Pakuti muli nonse mwa Khristu koma ngati muli a Khristu, muli mbewu ya Abrahamu, nyumba monga mwa lonjezano.***

Mulungu akanakhala ndi tsankho, ndiye kuti anthu amitundu (amene sanali Ayuda) sakanapulumuka.

4. Kusakhazikika

Pamene tiyesera kutanthauzira Mau a Mulungu, ndipo ife sindife okhazikika pa zochitika "ZAUZIMU", tikhonza kuyesedwa potanthauzira Baibulo molakwika.

a. Mchitidwe wokhazikika komanso wodzifufuza wekha komanso kulapa

Ife tikuuzidwa mu 2 Akorinto 13:5 kuti *"dziyeseni"* nokha ngati muli mu chikhulupiliro kapena simudziwa kodi za inu nokha". Ife tiyenera kuika osati zochita zathu zokha komanso zolinga zathu pamaso pa Ambuye ndi cholinga chofuna kufananiza ndi zimene Mulungu akufuna. Pamene tipeza kuti ife talephera, tiyenera kumuuza Ambuye zimene ife talephera ndikupempha kuyeretsedwa. 1 Yohane 1:9, amanena kuti *"ngati tivomereza machimo athu (iye) ali wakukhulupilika ndi wolungama kuti atikhululukire machimo athu ndi kutisambitsa kutichotsera chosalungama chiri chonse."* Kulephera kuchita chithu chimenechi, zikhonza kutipangitsa ife kukhala a umunthu chabe, zimene zimabweretsa kuononga ndi kulakwitsa pamene titanthauzira Mau a Mulungu.

b. Mchitidwe wokhazikika pa pemphero.

Ife tikuuzidwa pa Mateyu 7:7-8, kuti *"pemphani ndipo chidzapatsidwa kwa inu, funafunani mudzapeza, gogodani ndipo chidzatsegulidwa, pakuti yense wakupempha adzalandira, wogogoda chitsegulidwa ndipo wofunayo adzapeza".* Tiyenera kupemphera motsimikiza mtima wathu kuti timvetsetse komanso kusunga Mau a Mulungu. Kulephera kuchita chinthu ichi, kukhonza kubweretsa kuononga kwa ubale wathu ndi Mulungu Atate, amene Mau ake ndi amene ife tikuwamasulira.

c. Mchitidwe wokhazikika komanso wodzifufuza wekha komanso kulapa

Ife tikuuzidwa mu 2 Timoteo 2:15 kuti, *"uchite changu kudzionetsera kwa Mulungu wovomerezeka, wopanda chifukwa chochita manyazi, wolunjika nawo bwino mau a choonadi."* Kupanda chidwi powerenga mau kungasokoneze mamvekedwe a mauwo.

5. **Ndondomeko zolakwika**

Njira zina zomasulira mau zingathe kusokoneza katanthauzidwe kolondola pa Mau a Mulungu. Chikhulupiriro chathu pa mau ndichoti ndime ikhonza kupangitsa munthu kuti amamvetsetsa zinthu montani. Monga mwachitsanzo, ngati simukukhulupilira kuti Baibulo ndi mau ouzilidwa ndi mpweya wa Mulungu (2 Timoteo 3:16-17) ndiye kuti tikhonza kuganiza mwa nzeru zanthu pa zozizwa zimene zimene zimachitika. Ngati tikhulupirira, kuti Baibulo ndi lolondora, ndiye kuti zizizwa zonse ziyanera kumasulidwa ngati zimene Mulungu anchita mu mbiri.

Pali anthu ena omwe amakhulupilira kuti aKhristu ena owerengeka okha ndi omwe angathe kutanthauzira mau a mu Baibulo. komabe Baibulo limati okhulupilira onse ali ansembe (1 Petro 2:5, 9). Monga ansembe ali ndi kuthekera kofika ku mpando wa ulemelero wa Mulungu (Ahebri 4:16), kumene ife tingaphunzire mwachindunji ndi Mulungu Mzimu Woyera (1 Akorinto 2:15).

Anthu ena amaononga Mau a Mulungu pounikira njira zomasulira mau pamene mau amatanthauza zinthu zobisika komanso mwina nkhani zopeka pamene ndime zikukamba zinthu monga m'mene ziriri. Kukamba za zinthu zimene zikutanthauza zinthu zosaoneka, zikutanthauza kuti munthu wabweretsa tanthauzo lachilendo pa ndime. Ngait ife tikukamba za chigumula cha Nowa chinali kuti sichinali chisonyezo cha mavuto a padziko lonse lapansi (chigumula), koma chinali chithunzithunzi cha mazunzo amene anthu adziko lapansi akhonza kupirira, ndiye kuti ife tikhala ndi uchimo wotanthauzira zinthu potengera ndi zinthu zimene kulibe.

Kuunikira nkhani zopeka ndiko kutanthauzira choonadi chaching'ono ndi kukometsera kwambiri pokamba za choonadi chachikuru. Ngati tiona za chigumula cha Nowa, kuti chinali chaching'ono, chimene chinachitika dera lina lake ndipo pambuyo pake anthu ena mu mb'adwp akhonza kukometsera kuti izi zinakhudza anthu ambiri, ndiye kuti tikutanthauzira monga nkhani zopeka. Munthu wina akhonza kunena kuti pamene tikutanthauza mau poona za nkhani zopeka, ndiye kuti choonadi chaching'ono chazungululidwa ndi mmabodza ambiri.

Anthu ena amakhonzanso kukamba poona zinthu zimenezi kuti zikufanana ndi kumasulira zinthu zimene ziri zobisika komanso komanso kupeka nkhani ndi kukamba zimene pofanizira Yesu Khristu, Mtanda komanso kuuka kwake. Ngati kumasulira kumeneko kuli koona, ndiye kuti Yesu sanafere machimo athu kapena kuikidwa m'manda ndi kuukitsidwa ku chipulumutso chathu. Molingana ndi mtumwi Paulo, ife tiri pa mavuto akuru ngati zinthu zonse izi sizinachitike (1 Akorinto 15).

Kutanthauzira kwenikweni kwa zinthu monga m'mene ziriiri sikumaonetsa za zilankhuro zina zophiphiritsa zimene zimaononga za kamasulidwe ka Mau. Mwa chitsanzo, buku la nyimbo ya Solomo ndi chitsanzo choonekeratu chimene mukamasulira monga m'mene zinthu ziriri simungathe kumvetsesa. Molondora zinthu izi bwino lomwe, njira yabwino yomasulira ndiyakuti imakamba zomasulira molingana ndi m'mene zinthu ziriri zimene zimaonetsa za mau ophiphiritsa komanso kulankhura kokamba za zifanizo. Tikamba momveka bwino zinthu izi patsogolo.

6. **Kuganiza koipa**

Maganizidwe a umunthu sangathe kumvetsetsa za Mulungu wosaonekayo. Titakhala kuti tikumvetsetsa za m'mene Mulungu molingana ndi maganizo athu a umunthu, ife tikhala anthu osadziwa kanthu. Ife tikuuzidwa ku Miyamba 3:7-7 kuti ***"Khulupilira yehova ndi mtima wako onse, osachikinzika pa luntha lako, umlemekeze pa njira zako zonse ndipo iye azaongora mayendedwe ako, usaziyese wekha wanzeru, opa yehova, nupatuke ku zoipa"***. Mulungu akufuna ife tiyende mu chikhulupiliro osati mwa nzeru zathu zathupi.

Talonjezedwa kuti tsiku lina tidzakhala tsiku lina tidzamumvetsetsa Ambuye. Paulo analemba ku 1 Akorinto 13:12 kuti ***"Pakuti tsopano tipenya mukalilore ngati chimbudzi, koma pomwepo maso ndi maso, tsopano tizindikira mdera-mdera koma pomwepo tizazindikiratu monganso ine ndizindikiridwa."*** Mafunso onse osayankhidwa amene tili nawo okhudza Mau a Mulungu, kuti tsiku lina adzayankhidwa tikadzakumana maso ndi maso ndi Ambuye (2 Akorinto 3:18).

Ayuda a mu zaka zoyamba anali ndi mavuto pamene kudalira pa nzeru zawo, zimene zinabweretsa kulakwikwa kwakukuru kumene anthu sanazindikire Yesu monga Mesiya. Onani zokambirana pakati pakati pa Yesu ndi afarisi monga m'mene zalembedwera mu Mateyu 22:41-46:

> ***Ndipo pamene Afarisi anasonkhana, Yesu anawafunsa nati, muganiza bwanji za Khristu, ali mwana wa yani? Iwo ananena naye, ali mwana wa davide. Ndipo iye anati kwa iwo ndipo Davide mu uzimu atchura bwanji iye Ambuye nanena?- Ambuye ananena kwa ambuye wanga, ukhala kudzanja lamanja, kufikira ine***

tidzaika adani ako pansi pa mapazi ako. Cifukwa cace ngati Davide amchula Iye Ambuye, ali mwana wace bwanji? Ndipo sanalimbika mtima munthu aliyense kumfunsa kanthu kuyambira tsiku lomwelo.

Yesu anagwiritsa nchito Masalmo 110:1 pamene amafunsa Afarisi za m'mene Mesiya akhonza kukhaliranso mwana wa Davide komanso panthawi yomweyo Ambuye wa Davide. Yankho ndi lakuti Mesiya ndi Mulungu komanso munthu; ndipo kuganiza kumeneku kukoneka kuti ndikosiyana ndi m'mene munthu amaganizira, monga sichoncho?

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Chaputala 4, Gawo 4C

1. **Werengani 1 Akorinto 3:3, kodi ndi zinthu ziwiri ziti zimene Paulo anazitchula ngati za "kuthupi" komanso ku "umunthu"?**

2. **Agalatiya 5:19-21, Kodi kaduka ndi njiru ndi chiyani?**

3. **Kodi munthu wakaduka kapena njiru akhonza kusintha motani mamasulidwe a Mau?**

4. **Werengani Miyambo 3:5-6, 1 ndi Akorinto 8:1. Kodi sitiyenera kukhulupilira chiyani? Nanga ndi chifukwa chiyani?**

5. **Kodi ife tingakhale anthu osadziwa za m'mene tikhonza kukhalira ndi chizolowezi kapena njira yophunzirira ndi kukhala anthu akuthupi komanso amene ali olephera kumasulira mau?**

6. **Kodi timasulire Baibulo pogwiritsa ntchito malingaliro athu? Chifukwa chiyani?**

7. **Kodi chofunika kwambiri ndi chiyani pamene tiphunzira mau a Mulungu?**

8. **Werengani 2 Akorinto 13:5 ndi 1 Yohane 1:9. tchulani zinthu ziwiri zofunika pa maphunziro athu a mau?**

9. **Werengani Mateyu 7:7-8 ndi Yakobo1:5. Kodi ife tifunefune chiyani pamene tiphunzira mau?**

10. **Kodi ndi chifukwa chiyani tiyenera kukhazikika pophunzira?**

11. **Werengani 2 Timoteo 3:16-17. Kodi ife tikhulupilire zotani zokhuza Baibulo tisanayamebe kufufuza za matanthauzidwe abwino a mau?**

12. **Werengani Yesaya 55:8-9. Kodi tikumbukire chiyani pamene tifuna kugwiritsa ntchito nzeru zathu pa mau a Mulungu?**

13. **Werengani Yakobo 3:14. Kodi ndi zinthu zitatu ziti zomwe zimalepheretsa kutanthauzira mau?**

D. Njira Zisanu ndi Zitatu Zolepheretsa kugwiritsa ntchito Mau a Mulungu

Njira zisanu ndi zitatu zimenezi zaperekedwa mosavuta komanso ziyenera kutsatilidwa ndi wophunzira. Ndi chinthu chofunikira kuti tionenso ndime zina zimene ziri zolondora kuti zititsogolere. Tiyeni tioneni Miyambo 3:5-6 akuti, ***"Khulupilirani Mulungu ndi mtima wanu onse ndipo musadalire malingaliro anu.muzonse muvomereze iye ndipo adzalungamitsa njira zanu."***

1. **Kulephera Kudalira pa Ambuye kuti atipatse mphanvu yochita monga mwa Mau ake**
   Pakhonza kukhala nthawi zina zimene nzeru zathu ziri zolondora, komabe timayenera kuona kuti sitingathe kukhonza pa muyeso umenewu. Mwa chitsanzo, machimo a munthu amakhala oonekeratu, ndipo pamafunika munthu wina kuti athandize "ponyamula zolemetsa za wina" (Agalatiya 6:1-2), koma ife timalephera kuthandiza munthu amene ali ovutika.

2. **Kukana Kusintha za kuganiza ndi kuchita zimene zimatsutsa choonadi cha Mulungu**
   Pali zintsanzo zambiri za zimene mu Mau a Mulungu. Choyamba, zikuoneka pamene Yesu anabwera ku dziko kuno pamene Ansembe ndi Afarisi anaona munthu amene anali wosaona chibadwire atachiritsidwa, ndipo iwo anakana kukhulupirira za Iye amene anachita chozizwayo (Yohane 9:30-34).

3. **Kusamvera Mfundo zimene ziri zolondora**
   Adamu adauzidwa kuti asadye mtengo wina m'munda mwa Eden ndipo kuti akadya adzafa. Ichi ndi china mwa chitsanzo chosankha mwadala kusamvera.

4. **Kumamatira pa zimene dziko lapansi likufuna**
   Nkhondo yaikulu pa moyo wa chiKhristu ndiyo "kukonda za m'dziko lapansi" komanso zimenezi zikutha (1 Yohane 2:5-17). Izi zimachitika pamene munthu afuna: kutchuka, kupeza mwayi, kupeza mphamvu komanso zokondweretsa za thupi zimene anthu amazifuna pa moyo. Ena amfunitsitsa kuti adziwike, ena amafuna chuma, ena ulamuliro komanso chilakolako.

5. **Kulephera kukhala ndi chidwi kuchita Mau a Mulungu pa moyo**
   Kulephera uku ndi chitsanzo chimene chikuonetsedwa makamaka kwa iwo amene "achita zomwe ndi zolondora pamaso pa iwo eni" (Oweruza 17:6; 21:25). Izi ndi zomwe zaonetsedwa chifukwa cholephera kuyamikira chisomo cha Mulungu, komanso kulephera kuthokoza Mulungu monga m'mene akhoza kulandirira ulemu wake.

6. **Kuona ntchimo kuti liri monga mwa chilamulo komanso kapena kuti tchimolo palibe.**
   Anthu ena amaonjezera ku Mau a Mulungu, ndipo amatenga zinthu zimene iwo awonjezera zija kukhala mulingo wa moyo wauzimu. Afarisi amadziwika bwino pochita zimenezi, makamaka kukhala ndi malamulo ena amene amakhonza kukamba zosamba m'manja (Marko 7:1-4). Mulungu sanapereke njira ina iriyonse. Chitsanzo china ndi m'mene anthu amakhonza kuona kuti sitchimo pamene Mulungu walankhura mwa chindunji. Mwa chitsanzo ukwati wa athu ofana monga wamamuna kapena wamkazi, izi kwa ena zimaoneka kuti sitchimo (Aroma 1:26-32).

7. **Kusinthanitsa za zimene munthu umamva ndi zisankho zabwino.**
   Chilakolako ndi zimene amamva nthupi zimene zikhonza kupangitsa munthu kuti achite chigololo ngati sangathe kugwiritsa ntchito nzeru (Miyambo 5:1-6).

8 **Kunonga zimene munthu akuganiza chifukwa cha tsankho, kukondera kapena ulesi**
   Tonse ndife anthu ofanana pamaso pa Mulungu (Agalatiya 3:26-29), choncho kulephera kukonda mzathu pa malingaliro, machitidwe ndi malankhulidwe ndiko kuphwanya "malamulo aakulu awiri" (Marko 12:29-39)

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Chaputala 4, Gawo 4D

Werengani mosamalitsa ndipo mukhale ndi nthawi yabwino ndithu kuti muunikire moona mtima ngati pali kanthu kena kamene kakufunika kukonza m'moyo mwanu.

Mutu 5

Chiphunzitso cha Umunthu wa Mulungu

Gawo 1
Utatu Woyera wa Mulungu

A. Kafotokozedwe ka Utatu wa Mulungu

Timadziwa bwino kuti pali Mulungu m'modzi owona (Deutronomo 4:35; 6:4; 1 Akorinto 8:4-6; Aefeso 4:3-6; Yakobo 2:19) amene amazionesera kuti ndi Atate (Yohane 6:27), Mwana (Yohane 1:1) ndi Mzimu Woyera (Machitidwe 5:3-4). Koma ndizovuta kudziwa kagwiridwe ntchito kake.

Ndizovuta kudziwa bwinobwino komanso kupereka tanthauzo lenileni la atatu amene ali mwa Mulungu chifukwa choti Mulungu amaposa kaganizidwe kathu chifukwa iye ndi Mulungu (Aroma 11:33). Moyo wathu wa Chikhristu uyenera kukhala wachikhulupiliro kuti timukondweretse iye (Ahebri 11:6). Tikanakhala kuti timadziwa komanso kumvetsa chilichonse chokhuza Mulungu mmoyo uno bwenzi tikuyenda mwa thupi.Tsiku lina tidzamuziwa bwinobwino Mulungu (1 Akorinto 13:12) koma kwa nthawi ino tiyenera kuvomereza ndi chikhulupiliro chomwe sitimachimvesetsa bwinobwino. Kalongosoledwe kena ka utatu wa Mulungu kamapezeka mu dzira. Dzira lili ndi khungu, chachikasu komanso choyera, zigawo zitatu zosiyanasiyana komabe ndi dzira limodzi.

Tazindikira bwinobwino kuti utatu wa Mulungu uli ndi ntchito zitatu. Atate ndi amene amakonza zinthu (Machitidwe 2:23), Mwana ndi amene amachita zimene Atate amutuma (Yohane 5:36) komanso Mzimu Woyera amene amabvumbulutsa zinthu (Yohane 16:13). Pamene tikuphunzira kusiyana kwa ntchito zawo tisafune kugawa utatu wa Mulungu. Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera onse amagawana chikhalidwe chomwe Mulungu yekha angakhale nacho.

Ilili lisakhale vuto kwaife. Tikhoza osamvetsetsa momwe mkati mwa galimoto mumagwilira ntchito koma timaona zotsatira pamene taliza "Engine" ndi kuyendetsa kupita kumene tikufuna. Tikhoza kuona zotsatira zachikhalidwe cha Mulungu kuchokera ku zimene iye analenga (Aroma 1:20).

B. Umboni

Umboni wa utatu wa Mulungu umachokera pamene Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera amatchulidwa onse kuti ndi Mulungu zomwe tinaonetsa kale mu mfundo yapita ija. Ngati Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera ali ndi chikhalidwe chomwe Mulungu yekha angakhale nacho komanso amagwira ntchito zimene Mulungu yekha angagwire, ndekuti atatuwo ndi m'modzi yemwe ali Mulungu.

M'mutu wachinayi m'gawo loyamba "kutanthauza kutengera ukulu wake," upangiri wa Mulungu unafotokozedwa. Panopa tifotokoze bwinobwino chikhalidwe cha Mulungu komanso kulumikiza chikhalidwe chilichonse kwa utatu wa Mulungu. Zimenezi ndizofunika kwambiri kumbali yamaphunziro.

Mavesi amenewa amapanga zilumika ziwiri zofunikira mu phunziro la Baibulo zimene Mwana wasukulu aliyense ophunzira mau a Mulungu ayenera kuti asazaiwale. Choyambilira ndi chakuti, "pali Mulungu m'modzi yekha." Chachiwiri nchakuti, "Mulunguyo siine."

C. Zinthu Khumi Zimene Zimaonetsa Ukulu Wake

Bulaketi yoyambilirayi ( ) ikuonetsa ma:esi amene amaimilira Atate Mulungu; yachiwiri < > ma: esi a Mwana; komanso yachitatu [ ] Mzimu Woyera.

1. Mfumu ya Mafumu

Mulungu ndi mfumu ya mafumu, kutanthauza kuti ndi mfumu amene samalakwitsa (Danieli 4:17; 1 Timoteo 1:17; Masalmo 47:2, 7), <Chibvumbulutsso 19:16; Yohane 5:21>, [Zekaliya 4:6; 1 Petro 4:14; 1 Akorinto 12:11].

Mfumu ya mafumu akutanthauza "kukhala ndi mphamvu ya ulamuliro." Mulungu yemwe samalamulidwa ndi mphamvu ili yonse ndi amane ali ndi mphamvu zolamura zachilengedwe zonse. Iyeyo ndi mlengi osati olengedwa (Aroma 1:20, 25).

Mulungu ali ndi mphamvu yopanga zomwe iye wakonza, malamulo ake komanso chiweluzo chake. Mwachidule ali ndi mphamvu yopanga chimene iye wafuna, ngakhale zofuna zake nzovuta kuzimvetsa.

2. Wolungama

Mulungu ndi wolungama, kutanthauza kuti ndiwa ngwiro munjira iliyonse (Yohane 17:25; 1 Yohane 1:5), <1 Yohane 2:1; Luka 1:35; Ahebri 7:26>, [Yesaya 32:15-18; Masalmo 143:10; Nehemiya 9:20]. Iyeyo ndi muyeso weniweni wa kulungama. Khalidwe llake ndi labwino lomwe timayenera tilitsatire (Aefeso 5:1).

3. **Chilungamo**
Mulungu ndi wachilungamo. Iyeyo ndi chilungamo chonse (Yesaya 45:21; Yobu 37:23), <Yohane 5:22, 30; Chibvumbulutso 19:11>, [Yesaya 4:4; 28:6]. Chilungamo cha Mulungu chimagwirizana ndi kulungama kwake. Mulungu "alibe tsankho" (Aroma 22:11), samakondera. Pamene tchimo (lomwe liri kuphwanya malamulo ake) lachitika (Aroma 5:13), chilungamo chake chimachitika.

Munthu samafanana ndi kulungama kwa Mulungu ndiye amafuna mpulumutsi yemwe amakwaniritsa chilungamo cha Mulungu. Yesu Khristu anakwaniritsa pamena anafera pamtanda chifukwa chazochimwa za anthu onse a dziko lapansi (1 Yohane 2:1-2).

4. **Chikondi**
Mulungu ndi wa chikondi, kutanthauza kuti chikondi chabwino ndi chosatha chimapezeka mwa iye (1 Yohane 4:8-10; Tito 3:4; Yohane 17:24-26), <Yohane 15:9 >, [Agalatiya 5:22].

Chikondi cha Mulungu chotere ndi ndiye maziko anatumira mwana wake obadwa yekha kuzatipulumutsa ife (Yohane 3:16). Chikondi ndichimene analipilira ambuye Yesu chifukwa cha machimo athu. <Luka 23:43>. Ndipo ndi mphatso yoyamba ya Mzimu woyera [Agalatiya 5:22].

Chikondi chimatanthauza kuchita zinthu zolondora komanso zabwino kwa anthu ena, ngakhale iwe mwini sufuna. Akhristu ayenera asatire chikondi cha Mulungu ndikuchifalitsa kwa anthu ena kuti anthu onse amudziwe Mulungu (Yohane 13:34-35).

5. **Moyo Wosatha**
Mulungu ndi moyo wosatha. Anakhalapo ndipo adzakhalapo (Yesaya 57:15), <Yohane 8:54; 1 Yohane 5:11-12; Mika 5:22; Chibvumbulutso 1:8, 17>, [Ahebri 9:14].

Moyo wosatha ulibe chiyambi kapena mathero. Akhristu timakhala ndi moyo wosatha, womwe uli ndi chiyambi koma ulibe mathero. Moyo wosatha wa Mulungu umatiphunzitsa kuti iyeyo sangazafe.

6. **Wamphamvu Zonse**
Mulungu ndi wamphamvu zonse kutanthauza kuti ali ndi mphamvu yopanga chilichonse (Marko 14:36; 1 Petro 1:5), <Mateyu 28:18; Chibvumbulutso 19:6>, [2 Timoteo 1:7; Aroma 15:13].

Chitsanzo cha mphamvu zake chimaoneka kuchokera ku chilengedwe cha kumwamba ndi dziko lapansi (Genesis 1:1). Tinauzidwa kuti "mau a pakamwa pake" analenga kumwamba "mphweya" wake unalenga zonse zokhala kumwamba (Masalmo 33:6).

7. **Opezeka Paliponse**
Mulungu amapezeka paliponse kutanthauza kuti amapezeka paliponse nthawi zonse (Miyambo 15:3; 2 Mbiri 2:6), <Mateyu 18:20; 28:20>, [Masalmo 139:7-16]. Izi sizikutanthauza kuti Mulungu ndi chinachilichonse, koma kuti ali paliponse. Zikutionesera chikhalidwe cha Mulungu.

Taona kuti chikhalidwe cha Mulungu sichimasankha malo (Masalmo 139:7-17). Ndekuti Mulungu samakonda anthu ena kuposa ena. Mulungunso amapezeka malo osiyanasiyana kwa nthawi imodzi.

8. **Odziwa Zonse**
Mulungu amadziwa chilichonse: chakale, chatsopano komanso chamtsogolo (Masalmo 139:1-6; Ahebri 4:13), <Yohane 2:24, 25; 18:4; Mateyu 9:4>, [1 Akorinto 22:10-11; Yesaya 11:2].

Amadziwa chotsatira cha zinthu zonse; osati zochitika zokha komanso zimene zikhoza kuchitika. Amadziwa zotsatira za zisankho zomwe tachita nthawi zonse. Chikonzero chaka chosatha chinaona zonsezo (Aroma 8:28 -30).

9. **Osasintha**
Mulungu ndi osasintha kutanthauza kuti ukulu wake sumasintha (Yakobo 1:17; Ahebri 6:17; Malaki 3:6), <Ahebri 13:8>, [1 Akorinto 12:4; Aefeso 1:13].

Chikhalidwe chimenechi nchofunikira kwambiri kwa munthu, chifukwa Mulungu amayenera kuchita nthawi zonse zomwe analonjeza, sangasinthe maganizo ake. Chifukwa chake ananena kuti ***"iwo akukhala mwa Khristu Yesu alibe kutsutsidwa"*** (Aroma 8:1), choncho tikhoza kukhala ndi chikhulupiliro ndi kulimbika mtima kuti sangasinthe maganizo ake. Analonjeza moyo wosatha kwa amene amakhulupiulira Yesu Khristu; ndiyeno tikudziwa kuti sangasinthe uthengawu (Yohane 3:16).

Ngati Mulungu angasinthe malonjezano ake, ndekuti akhoza kukhala wabodza, zomwe zingamupange kukhala osalungama (Ahebri 6:17-18).

Chinachilichonse padziko lapansi chikusintha ndi Mulungu yekha yemwe sakusintha. Ichi nchifukwa chake mwa iye tiyembekezamo kupezamo chipulumutso (Ahebri 6:19).

10. **Wachilungamo**
Mulungu ndi wachilungamo chokwanira (Deutronomo 32:4; Yohane 7:28; 17:3), <Yohane 14:6; 1 Yohane 5:20>, [1 Yohane 5:7, 8; 4:6; Yohane 14:17; 15:26; 16:13].

Chikhalidwe chimenechi chimatiuza kuti chinachilichonse chimene Mulungu angapange nchokhulupilika (Numeri 23:19). Sizingatheke kuti Mulungu aname (Tito 1:2).

Chilungamo ndichakuti Mulungu anazionesera yekha mu umunthu wa Yesu Khristu <Yohane 14:6>. Tikasatira mbiri, chilungamo chinkaoneka kudzera mu mfundo zimene zinali ndi umboni, kayankhulidwe kapena lamulo. Ichi nchifukwa chake chilichonse chimene munthu amaona kuti ndi chilungamo, chiyenera kusiyanitsidwa ndi mau a Yesu Khristu <1 Timoteo 6:3>.

Zoyenera kuchita aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Mutu 5, Gawo 1

1. **Choyamba Werengani Deutoronomu 6:4-5, kenako Yohane 6:27, 1:1 ndi Machitidwe 5:3-4. Kodi Milungu yoona iripo ingati?**

2. **Kuchokera mu kuwerengaku, Mulungu ndi ndani?**

3. **Werengani Machitidwe 2:23. Kodi ntchito yeniyeni ya Atate ndi yotani?**

4. **Werengani Yohane 5:36. Kodi ntchito yeniyeni ya Mwana ndi yotani?**

5. **Werengani Yohane 16:13-14. Kodi ntchito yeniyeni ya Mzimu Woyera ndi yotani?**

6. **Tingasonyeze bwanji kuti Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera ndi Mulungu M'modzi?**

7. **Werengani nkhani za ukulu wa Mulungu:**
   a. Atate –Daniel 4:17, 1 Timoteo 1:17 ndi Masalimo 42:2, 7
   b. Mwana–Chibvumbulutso 19:16 ndi Yohane 5:21
   c. Mzimu Woyera–Zekariya 4:6, 1 Petro 4:14 ndi 1 Akorinto 12:11

   Kodi utatu woyera wa Mulungu ukusonyezadi mphamvu ndi ukulu wake?

8. **Werengani nkhani za chilungamo cha Mulungu:**
   a. Atate –1 Yohane 17:25 ndi 1 Yohane 1:5
   b. Mwana –1 Yohane 2:1, Luka 1:35 ndi Ahebri 7:26
   c. Mzimu Woyera–Yesaya 32:15-18, Masalimo 143:10 ndi Nehemiya 9:20

   Kodi Utatu wa Mulungu ndi wolungamadi?

9. **Werengani nkhani za kukhulupirika ndi kuona mtima kwa Mulungu:**
   a. Atate–Yesaya 45:21 ndi Yobu 37:23
   b. Mwana–Yohane 5:22, 30 ndi Chibvumbulutso 19:11
   c. Mzimu Woyera–Yesaya 4:4 ndi 28:6

   Kodi utatu wa Mulungu ndi wokhulupirika ndi woona?

10. **Werengani nkhani za chikondi cha Mulungu:**
   a. Atate–1 Yohane 4:8-10, Tito 3:4 ndi Yohane 17:24-26
   b. Mwana–Yohane 15:9
   c. Mzimu Woyera–Agalatiya 5:22

   Kodi Utatu wa Mulungu uli nacho chikondi chenecheni?

11. Werengani nkhani za moyo wamuyaya wa Mulungu.

a. Atate–Yesaya 57:15
b. Mwana–Yohane 8:54, Yohane 5:11-12, Mika 5:2 ndi Chibvumbulutso 1:8, 17
c. Mzimu Woyera–Ahebri 9:14

Kodi Utatu wa Mulungu uli nawo moyo wamuyaya?

12. Werengani nkhani za Mulungu wa mphamvu yonse:

a. Atate–Marko 14:36 ndi 1 Petro 1:5
b. Mwana–Mateyo 28:18 ndi Chibvumbulutso 19:6
c. Mzimu Woyera–2 Timoteyo 1:7 ndi Aroma 5:13

Kodi Utatu wa Mulungu ndi wa Mphamvu yonse?

13. Werengani nkhani za kupezeka paliponse kwa Mulungu:

a. Atate–Mika 15:3 ndi 2 Mbiri 2:6
b. Mwana– Mateyu 18:20 ndi 28:20
c. Mzimu Woyera–Masalimo 139:7-16

Kodi Utatu wa Mulungu uli wopezeka paliponse?

14. Werengani nkhani za Mulungu wodziwa zonse:

a. Atate–Masalimo 39:1-6 ndi Ahebri 4:13
b. Mwana–Yohane 2:24-25, 18:4 ndi Mateyu 9:4
c. Mzimu Woyera–1 Akorinto 2:10-11 ndi Yesaya 11:2

Kodi Utatu wa Mulungu ndi wodziwa zonse?

15. Werengani nkhani za Mulungu wosasinthika:

a. Atate– Yakobo 1:17, Ahebri 6:17 ndi Malaki 3:6
b. Mwana– Ahebri 3:8
c. Mzimu Woyera– 1 Akorinto 12:4 ndi Aefenso 1:13

Kodi Utatu wa Mulungu ndi wosasinthasintha?

16 Werengani nkhani za choonadi cha Mulungu:

a. Atate–Deutoronomu 32:4, Yohane 7:28 ndi 17:3
b. Mwana–Yohane 14:6 ndi 1 Yohane 5:20
c. Mzimu Woyera–1 Yohane 5:7-8, 4:6, Yohane 14:17, 5:26 ndi 16:13

Kodi Utatu wa Mulungu ndi wa choonadi?

Gawo 2
Maina a Mulungu

Gawo ili lafotokoza maina a Mulungu amene amapezeka m'malemba. Pali maina osiyanasiyana a Mulungu mu chiyankhulo cha Greek komanso Hebri amene amagwiritsidwa ntchito posiyanitsa chikhalidwe chake.

Muchitanthauziro china mau a mu chi Hebri kapena Greek anasinthidwa nchiyankhulo chatsopano (chomwe chimatchulidwa kuti transteritaration), kutengera muchiyankhulo chawo osati m'mene akuwamvetserera. Phunziro ili limamupatsa Mwana wa sukulu maina enieni a mu chi Hebrew kapena Greek komanso kamasulidwe kawo.

A. Maina a Chi Hebri

1. Mulungu

Mau a chi hebri amene amatanthauza Mulungu ndi ELOHIM. Anapezeka koyambilira mu Genesis 1:1 kenako oposa zikwi ziwiri ndi mazana asanu mu chipangano chakale. Kutanthauza kwa mau awa nkokuti ukulu wonse wa Mulungu. Pamene dzinali lagwiritsidwa ntchito kwambiri kutchura Atate, Mwana wa sukulu ayenera awone kuti dzinali limagwiritsidwanso ntchito pomutchura Mwana ndi Mzimu Woyera chifukwa atatuwa ndi Mulungu.

ELOHIM ndi mau amene amatanthauza zambiri, amene analongosoledwa ndi anthu ophunzira ngati "kuchulukitsa kwa mfumu," kuonetsera mphamvu zake zosatha. Liwu ili ngakhale limaimira zinthu zambiri, limagwira ntchito ngati limodzi, zomwe zimaonetsa kuti pali Mulungu m'modzi yekha (Deutronomo 6:5).

Mawu oti ELOHIM amagwirizana ndi mau ena amene amapereka uthenga okhuza Mulungu komanso amakhala dzina lina la Mulungu.

a. Mulungu wa Mphamvu

"Mulungu wa mphamvu" anatanthauzidwa kuchokera ku EL SHADDAI. "EL" ndikufupikitsa kwa ELOHIM. Limagwiritsidwa ntchito pofuna kutchura madalitso amene Mulungu amawapatsa anthu ake. Limapezeka ku: Genesis 17:1; 28:3; 35:11; 43:14; 48:3; 49:25; Eksodo 6:3; Numeri 24:4, 16; Rute 1:20, 21; Yobu 5:17; 6:4, 14; 8:3, 5; 11:7; 13:3; 15:25; 21:15, 20; 22:3, 17, 23, 25, 26; 23:16; 24:1; 27:2, 10, 11, 13; 29:5; 31:2, 35; 32:8; 33:4; 34:10, 12; 35:13; 37:23; 40:2; Masalmo 68:14; 91:1; Yesaya 13:6; Ezekiel 1:24; 10:5; Yoweli 1:15.

b. Mulungu wa m'Mwambamwamba

Mulungu wa m'mwambamwamba anatanthauzilidwa kuchokera ku EL ELYON, Kutanthauza kuti wamphamvu zonse ku zinthu zonse. Limapezeka ku: Genesis 14:18, 19, 20, 22; 40:17; Numeri 24:16; Deutronomo 26:19; 28:1; 32:8; Yoswa 16:5; 2 Samueli 22:14; 1 Mafumu 9:8; 2 Mafumu 15:35; 18:17; 1 Mbiri 7:24; 2 Mbiri 7:21; 8:5; 23:20; 27:3; 32:30; Nehemiya 3:25; Masalmo 7:17; 9:2; 18:13; 21:7; 46:4; 47:2; 50:14; 57:2; 73:11; 77:10; 78:17, 35, 56; 82:6; 83:18; 87:5; 89:27; 91:1, 9; 92:1; 97:9; 107:11; Yesaya 7:3; 14:14; 36:2; Yeremiya 20:2; 36:10; Maliro 3:35, 38; Ezekieli 9:2; 41:7; 42:5.

c. Mulungu wa Muyaya

Kafotokozedwe ka dzina loti Mulungu wa muyaya kanatanthauzidwa kuchokera ku EL OLAM. OLAM ndi mau a mu chi Hebri amene amatanthauza kuti chosatha (chopanda chiyambi ndi mathero). Limapezeka ku Genesis 21:33 komanso Yesaya 40:28. Kusatha kwa Mulungu kunafotokozedwa kwambiri pamene mau a "muyaya" (OLAM) amapezeka.

2. Mbuye

YAHWEH amatanthauzidwa kuti MBUYE amene amalembedwa mu zilembo zikuluzikulu kuti asiyanitsidwe ndi mau ena amene amatanthauzidwa kuti "Mbuye" kapena "mbuye." YAHWEH amaphatikizidwa ndi mau ena kuti afotokoze umunthu wake ndi ntchito zake.

Dzina la Mulungu loti MBUYE linatanthauzidwa kuchokera ku mau a chi Hebrew otchedwa YAHWEH. YAHWEH ndi dzina la Mulungu (Eksodo 3:14) ndipo linagwwiritsidwa ntchito koposa ka chikwi kasanu ndi dzana zitatu mu chipangano chakale. Limationetsera kuti Mulungu alipo. Kagwiritsidwe ntchito ka MBUYE koyamba kamapezeka ku Genesis 2:4 kumene analilumikiza ndi ELOHIM ndikuli tanthauza kuti AMBUYE MULUNGU.

Dzina la Mulungu linakhara lofunikira kwambiri ku Israeli pamene amachokera ku ukapolo ku Babeloni mu zaka za (568–516 Yesu asanabadwe) ndipo samalitchura koma amamuitana kuti ADONAI. Kuchokera mu zaka za mma 600-700 Yesu atangomwalira, malemba owelengera (vowel), ADONAI, inaphatikizidwa ndi konsonanti (mawu osawerengera), YHWH, kupanga dzina loti "YEHOVA" kuwakumbutsa anthu owerenga kuti azitchura YHWH ngati ADONAI.

a. Ambuye Opatsa

AMBUYE opatsa anatanthauzidwa kuchokera kudzina loti YAHWEH JIREH. Dzinali limapezeka ku Genesis 22:14 ndipo limatsonyeza nthawi imene Mulungu anamupatsa Abraham Mwanawankhosa kuti apereke nsembe m'malo mwa Mwanawake ISAKI.

b. Ambuye ndi Mbendera yanga

AMBUYE ndi mbendera yanga, anatanthauzilidwa kuchokera ku dzina loti YAHWEH NISSI. Dzinali limapezeka ku Eksodo 17:15 lomwe linaperekedwa kwa Mulungu ndi Mose atawagonjetsa ma Amaelekaitsi.

c. Ambuye ndi Mtendere

Dzinali "AMBUYE ndi mtendere" linatanthauzidwa kuchokera ku YAHWEH SHAROM. Linagwiritsidwa ntchito ku Oweluza 6:24.

d. Ambuye wa Mphamvuyonse

Ambuye wamphamvu yonse ndi kumasulira kwa mawu a YAHWEH SABBAOTH, amene amagwiritsidwa ntchito ku nkhondo kutanthauza kuti Mbuye wolamulira ankhondo kuphatikiza a nkhondo a ngelo komanso ankhondo a Israel. Poyamba anagwiridwa ntchito ku 1 Samueli 1:3 kenaka mazana mazama.

3. Amuye a Chikhamu

ADONAI ndi mau oyimilira zambiri ngati mau a ELOHIM, amene amaonetsa ufumu wa Mulungu. Kusiyana ndi ELOHIM, ADON amaimira chinthu chimodzi. Mau oti ADON amatanthauza kuti Mulungu kusonyeza kuti mwini. Limagwiritsidwa ntchito kusonyeza mphamvu kapena ulamuliro. Linagwiritsidwa ntchito koyamba ku Genesis 18:3 pamene Abraham analigwiritsa ntchito pomutchura Mulungu.

Muchigiriki ifanizira Kurios.

B. Maina a Mu Chi Greek

1. Mulungu

Dzina la Mulungu mu Greek ndi THEOS. Ngati dzina la chi Hebrew, ELOHIM, dzinali limaimira Mulungu m'modzi. Ndi dzina lomwe limasankhidwa kwabiri kutanthauzira ELOHIM mu chi seputiganti (kutanthauzira chipangano chakale chamuchi hebri nkuchipititsa mu Greek).

Yohane 1:1 tomwe imafanana ndi Genesis 1:1, timapeza kuti mau oti ETHOS amagwiritsidwa ntchito m'malo mwa ELOHIM, kuonetseratu ubale wawo.

2. Ambuye

Mau a mu chi Greek a MBUYE ndi KURIOS. Linagwiritsidwa ntchito koposa ka mazana asanu ndi awiri mu chipangano chatsopano ndipo limaonetsa ulamuliro komanso ulemelero. Dzinali likhozanso kugwiritilitsidwa ntchito ngati dzina la ulemu.

Tinaona mu mfundo yapita ija kuti THEOS ndi ELOHIM amatanthauza chinthu chimodzi. Tinaonanso kuti KURIOUS ndi YAHWEH ali ndi tanthauzo limodzi. Ku marko 11:9, olemba analemba zimene zinalembedwa ku Masalmo 118:26, zomwe zimati ***"odalitsidwa ndi amene amadza mu dzina la Mulungu."*** Mudzina la chi Hebri ku Masalmo 118 ndi YAHWEH pamene dzina lomwe linatanthauzilidwa ndi KURIOS.

3. Mfumu ya Mafumu

Mfumu ya mafumu ndi tanthauzo lochokera ku mau oti wamkulu, ngakhale nthawi zina limatanthauzidwa kuti "MBUYE" (Luka 2:29; Machitidwe 4:24). Mfumu ya mafumu amayang'anitsitsa kwambiri kwa umwini osati ulamuliro ndi ulemelero zomwe zimatsogozedwa kwambiri ndi KURIOS. Limapezeka ku 1 Timoteo 6:1, 2; 2 Timoteo 2:21; Tito 2:9; 1 Petro 2:18; 2 Petro 2:1; Yuda 1:4; Chibvumbulutso 6:10.

Zoyenera kuchita aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Mutu 5, Gawo 2

1. **Fananitsani moyenera Maina a Mulungu a mu Chihebri:**

a. Mulungu	1) YAHWEH SABBAOTH
b. Mulungu wa Mphamvu zones	2) YAHWEH NISSI
c. Mulungu wamwambamwamba	3) ELOHIM
d. Mulungu Wamuyaya	4) ADONAI
e. Ambuye	5) EL SHADDAI
f. Ambuye Wopereka	6) YAHWEH SHALOM
g. Ambuye nyali yanga	7) EL OLAM
h. Ambuye wa mtendere	8) EL ELYON
i. Ambuye wamakamu	9) YAHWEH
j. Ambuye ndi mwini/bwana	10) YAHWEH JIREH

2. **Fananizani Maina Mulungu a mu Chigiriki:**

a. Mulungu	1) KURIOS
b. Ambuye	2) DESPOTES
c. Bwana	3) THEOS

Gawo 3
Mulungu Atate (-Chiphunzitso chokamba za Atate- Paterology)

A. Umunthu Wake

Njira yabwino yofotokozera Atate ndi kuona maina amene anawagwiritsa ntchito pozitchura iye mu mau ake. Mu phunziro lathu la utatu wa Mulungu lomwe tamaliza, taona kuti Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera amagawana chikhalidwe chimodzi. Panopa tigwiritsa ntchito kafotokozedwe komwe Buku loyera linagwiritsa ntchito potiphunzitsa ife za Atate wathu akumwamba.

Dziwani kuti ngakhale pali kusiyana pakati pa Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera pali Mulungu m'modzi (Deutronomo 6:4). Nthawi zambiri m'malemba, ndizovuta kudziwa kuti uti mwa atatuwo amene vesi ikumukamba. Kuvutaku kuli chonchi chifukwa Mulungu sangasiyanitsidwe kapena kugawidwa (Yohane 10:30; 14:9). Mu kafukufuku wa umunthu wa Atate, mau komanso malemba asankhidwa kuti awonjezere kamvetsetsedwe komanso kufunika kwa iye.

Nthawi zambiri mau afotokaza monga "wanga" amagwiritsidwa ntchito ndi "Atate." Izi zimachitika kufuna kusonyeza chikhalidwe cha Atate pamene mau monga "wako", "wake" kapena "wanga" aonjezeledwa ku mau a "Atate" zimaonetsera ubale wa munthu ndi Mulungu umene ulipo. Pamene mau oimira zambiri monga "athu", "anu" kapena "awo" aonjezeledwa amaonetsa ubale wagulu.

B. Kufotokoza za Umunthu Wake

- **"Wamphamvu"** zonse yomwe imakamba za mphamvu komanso kuthekera kwake kodalitsa. Genesis 49:25; Numeri 24:4, 16; Rute 1:20, 21; Yobu 5:17; 6:4, 14; 8:3, 5; 11:7; 13:3; 15:25; 21:15, 20; 22:3, 17, 23, 25, 26; 23:16; 24:1; 27:2, 10, 11, 13; 29:5; 31:2, 35; 32:8; 33:4; 34:10, 12; 35:13; 37:23; 40:2; Masalmo 68:14; 91:1; Yesaya 13:6, Ezekieli 1:24; Yoweli 1:15; Chivumbulutso 1:8
- **"Analipo kuyambira kale"** zomwe zikutionetsa umoyo wake wosatha. Danieli 7:9, 13, 22
- **"Mulungu wamuyaya"** zomwe zikutionetsa umoyo wake wosatha. Genesis 21:33; Yesaya 40:28
- **"Mulungu okhulupilika"** zomwe zikutionetsa kuti chikondi chake sichisintha. Deutronomo 7:9
- **"Atate a ulemelero"** zomwe zikutanthauza kuti ulemelero onse umachoka kwa iye. Aefeso 1:17
- **"Atate a chifundo"** zimene zikufuna kutionetsa chisomo chake. 2 Akorinto 1:3
- **"Mulungu wa m'mwambamwamba"** zomwe zikutanthauza kuti ali ndi mphamvu za ulamuliro pa dziko lapansi. Genesis 14:18, 19, 20, 22; Masalmo 57:2; 78:35; Ahebri 7:1
- **"Mulungu wa chifundo…wopanda chinyengo"** zomwe zikutanthauza kuti samalakwitsa. Deutronomo 32:4
- **"Mulungu wa ulemelero"** zomwe zikutionetsa umoyo wake wabwino. Masalmo 29:3; Machitidwe 7:2
- **"Mulungu wa milungu yonse"** zomwe zikutanthauza kuti mphamvu zake zimapotsa milungu yonse yadziko lapansi. Deutrronomo 10:17; Masalmo 136:2; Danieli 2:47; 11:36
- **"Mulungu wa mtendere"** zomwe zikutanthauza kuti Mulungu safunamkangano. Aroma 15:33; 16:20; Afilipi 4:9; 1 Atesalonika 5:23; Ahebri 13:20
- **"Mulungu wa moyo"** zomwe zikutanthauza umoyo wake wosatha. Mateyu 22:32; Marko 12:27; Luka 20:38
- **"Mulungu wa m'mwamba"** zomwe zikutanthauza kuti chilichonse timayang'anira kwa iye. Mika 6:6
- **"Mulungu wa chilungamo"** kutanthauza kuti chilungamo ndi chake. Masalmo 31:5; Yesaya 65:16
- **"Mulungu wa mkulu ndi wodabwitsa"** zomwe zikutanthauza ukulu ndi ufumu wake. Deuteronomu 7:21; Nehemiya 1:5; Danieli 9:4
- **"Mulungu wamkulu ndi wamphamvu"** zomwe zikutanthauza kuti ndi wamkulu komanso wa mphamvu. Yeremiya 32:18; Nehemiya 9:32
- **"Pakuti Yehova ndiye Mulungu wamkuludi Mfumu yaikuru yoposa milingu yonse"** zomwe zikuthandauza ukulu ndi ufumu wake. Masalimo 95:3
- **"Iye amene ayenera kuopedwa"** zomwe zikutanthauza kuti ayenera kupatsidwa ulemu. Masalmo 76:11, 12
- **"Woyera"** zomwe zikutionetsa kuti iye ndi woyera. 2 Mafumu 19:22; Yobu 6:10; Masalmo 22:3; 71:22; 78:41; 89:18; Miyambo 9:10; 30:3; Yesaya 1:41; 5:19, 24; 10:17, 20; 12:6; 17:7; 29:19, 23; 30:11-12, 15; 31:1; 37:23; 40:25; 41:14, 16, 20; 43:3, 14-15; 45-11; 47:4; 48:17; 49:7; 54:5; 55:5; 60:9, 14; Yeremiya 50:29; 51:5; Ezekiel 39:7; Hoseya 11:19, 12; Habakuku 1:12; 3:3; 1 Yohane 2:20
- **"Wansanje"** zomwe zikutanthauza kuti samafuna anthu ake azipembeza milungu ina. Eksodo 34:14

- **"Mulungu wa nsanje ndi obwenzera"** zomwe zikutanthauza kuti adzaweluza onse amene amafuna kusocheletsa anthu ake. Nahumu 1:2
- **"Mfumu ya ulemelero"** zomwe zikutanthauza kuti mpando wake uyenera ulemelero. Masalmo 24:7, 8, 9, 10
- **"Mulungu wa moyo ndi owona"** zomwe zikutanthauza chilungamo ndi kusatha kwake. 1 Atesalonika 1:9
- **"Ambuye Mulungu wamphamvu zonse"** zomwe zikutanthauzira ufumu wake (AMBUYE), chilengedwe (MULUNGU) komanso mphamvu zake. Chivumbulutso 4:8; 11:17; 15:3; 16:7; 21:22
- **"Mtendere"** zomwe zikuonetsa mtendere wake wosatha. Oweruza 6:24
- **"Ambuye wam'mwambamwamba"** zomwe zikutanthauza kuti ali ndi mfumu ya mafumu amene alipo. Masalmo 7:17; 47:2
- **"Mulungu wathu "** zomwe zikutandauza umuthu wake umene ulipo. Masalimo 90:17; Danieli 9:9, 15; Marko 12:29; Machitidwe Athumwi 2:39
- **"Chikondi"** zomwe zikutanthauzira chikondi chosatha chopezeka mwa iye. 1 Yohane 4:8, 16
- **"Wokoma mtima"** zomwe zikutionetsera kukhulupilika kwa chikondi chake. Eksodo 34:6, 7; Deutronomo 5:10, 7:9, 12; 1 Mafumu 8:23; 1 Mbiri 16:34; 2 Mbiri 6:14; Ezara 3:11; Nehemiya 1:5; 9:17; Yobu 37:13; Masalmo 6:4; 13:5; 26:3; 31:16; 32:10; 36:5, 7; 63:3; 89:2, 14; 103:8, 11; 136:1, 2-26; 138:8; Maliro 3:22, 32; Yoweli 2:13
- **"Mfumu ya ulemelero"** zomwe zikutanthauza ubwino wa chilengedwe chake. 2 Petro 1:17
- **"Mfumu ya kumwamba"** zomwe zikuonetsa ufumu wake. Ahebri 1:3; 8:1
- **"Iye ndi mfumu"** zomwe zikuonetsa chipambano cha ufumu wake.Yesaya 33:21
- **"Wam'mwambamwamba"** kusonyeza kuti iye amaposa zonse. Numeri 24:16; Deutronomo 32:8; 2 Samueli 22:14; Masalmo 7:17; 9:2; 18:13; 21:7; 46:4; 47:2; 50:14; 57:2; 73:11; 77:10; 78:17, 35, 56; 82:6; 83:18; 87:5; 91:1, 9; 92:1; 97:9; 107:11; Yesaya 14:14; Maliro 3:35, 38; Danieli 3:26; 4:2, 17, 24, 25, 32, 34; 5:18, 21; 7:18, 22, 25, 27; Hoseya 7:16; 11:7; Marko 5:7; Luka 1:32, 35, 76; 6:35; 8:28; Machitidwe 7:48; 16:17; Ahebri 7:1
- **"Nyimbo yanga"** kusonyeza kuti ndi chida changa. Eksodo 15:2; Masalmo 118:4; 119:54; Yesaya 12:2
- **"Mulungu ndi yekha"** zomwe zikutanthauza kuti palibenso Mulungu wina. Yohane 5:44; 1 Timoteo 1:7; Yuda 1:25
- **"Mulungu yekha wanzeru"** zomwe zikutanthauza kupambana kwa nzeru zake. Aroma 16:27
- **"Wabwino"** kutanthauza kuti palibe banga kapena tchimo mwa iye. Mateyu 5:48
- **"Mulungu owona"** kutanthauza kuti analenga munthu koma osati munthu analenga iye. 2 Mbiri 15:3; Yeremiya 10:10; 1 Yohane 5:20

C. Ntchito za Atate

Nchito za Atate mu utatu wa Mulungu zimakhuza chikonzero chimene iye anachikhazikitsa asanalenge kumwamba ndi dziko lapansi (Aefeso 1:11; 3:11).

D. Kufotokoza Ntchito za Atate

- **"M'misiri"** zomwe zikutanthauza kuthekera kwake kokonza ndikupanga mudzi wokhala nao maziko okhala ndi kuthekera kokhala ndi mphamvu kunja ndi m'kati mwache, maonekedwe ake komanso ubale pa gawo lililonse la mudziwo. Ahebri 11:10
- **"Womanga"** zomwe zikutanthauzira kuthekera kwake kosintha dongosolo kukhala chochitika. Ahebri 3:4; 11:10
- **"Mulungu wa chifundo ndi chisomo"** zomwe zikutanthauzira kuti iye ndi woleza ndi wakukoma mtima kochuluka. Eksodo 34:6.
- **"Mtetezi kwa osowa chitetezo"** kutanthauza kuti samakondwera ndi anthu amphamvu kapena ulamuliro wadziko lapansi amene amazunza anthu opanda mphamvu. Yesaya 25:4
- **"Mfumu yosatha"** zomwe zikutanthauza kusatha kwa ufumu wake. Yeremiya 10:10
- **"Tate wakuwala"** kusonyeza kuti iye amapereka mphatso zowalitsa dziko lapansi. Yakobo 1:17
- **"Tate wachifundo"** kutanthauzira chisomo chimene amapereka kwa zolengedwa zake. 2 Akorinto 1:3
- **"Tate wa mizimu"** kutanthauza kuti amapereka mphatso ya moyo wa uzimu kwa amene amakhulupilira Yesu Khristu. Ahebri 12:9
- **"Tate wa amasiye"** zomwe zikusonyeza chikondi chake kwa amasiye. Masalmo 68:5

- "**Mulungu okhululuka**" zomwe zikutanthauza kufuna kwake kopulumutsa anthu ku zochimwa zawo. Nehemiya 9:17; Masalmo 99:8
- **"Kasupe wa madzi a moyo"** kutanthauza kuti iye ndi amene amapereka ndi kusunga moyo wosatha. Yeremiya 2:13; 17:13
- **"Mpesa"** kutanthauza chidwi chake chopereka chipaso cha uzimu. Yohane 15:1
- **"Ulemelero wa Israeli"** kusonyeza kukhulupilika kwake komanso kukhazikika kwake kwa ana a Israeli. 1 Samueli 15:29; Mika 1:15
- **"Mulungu ndi Atate wa AMBUYE wathu Yesu Khristu"** kutanthauza chilengedwe cha thupi la Yesu Khristu. Aroma 15:6; 2 Akorinto 1:3; Aefeso 1:3; 1 Petro 1:3
- **"Mulungu ondilenga ine"** zomwe zikusonyeza kuti iye ndi amene analenga munthu .Yobu 35:10
- **"Mulungu ndi thanthwe langa"** kusonyeza kuti samasiya okhulupilira iye. Masalmo 42:9
- **"Mulungu wa Abraham, Isaki ndi Yakobo"** zomwe zikusonyeza pangano la Mulungu ndi Abraham. Eksodo 3:16; Machitidwe 3:13; 7:32
- **"Mulungu wachitonthozo chonse"** kutanthauzira ku chithandizo chimene iye amapereka pa nthawi yamavuto. 2 Akorinto 1:3
- **"Mulungu wa zamoyo zonse"** kusonyeza kuti ndi iye amene analenga anthu onse. Yeremiya 32:27
- **"Mulungu opereka chiyembekezo"** kusonyeza chiyembekezo chimene tili nacho mu dongosolo lake la mtsogolo. Aroma 15:13
- **"Mulungu wa chikondi ndi mtendere"** kusonyeza kufuna kwake kothetsa mkangano. 2 Akorinto 13:11
- **"Mulungu wa chipulumutso changa"** kutanthauzira chilengedwe cha munthu kapena umunthu pa pa chipulumutso chosatha. Masalmo 18:46; 25:5; 27:9; 51:14; 88:1; Mika 7:7; Habakuku 3:18; Luka 1:47
- **"Mulungu wa mphamvu zanga"** kutanthauza chilengedwe cha munthu kapena umunthu ndi chithandizo cha Mulungu kwa anthu. Masalmo 43:2
- **"Mulungu wakubwezera"** kutanthauza kuti azaweruza onse ochimwa. Yeremiya 51:56
- **"Mulungu wa mizimu ya za moyo zonse"** kutanthauza kuti amathandiza zamoyo zonse zolengedwa. Numeri 27:16
- **"Mulungu Atate wathu"** kutanthauza ubale umene omukhulupilira ali nawo ndi iye. Aroma 1:7; Akorinto 1:3; 2 Akorinto 1:2; Agalatiya 1:3; Aefeso 1:2; Afilipi 1:2; Akolose 1:2; 2 Atesalonika 1:1; 2:16; Filemoni 1:3; Yakobo 1:27
- **"Mulungu wa mphamvu zathu"** kutanthauza kuti samapereka mphamvu kwa munthu m'modzi koma anthu onse. Masalmo 81:1
- **"Mulungu wa maufumu onse a dziko la pansi"** kutanthauza kuti mphamvu zake zimaposa mphamvu zonse zopangidwa ndi angelo kapena munthu. 2 Mafumu 19:15; Yesaya 37:16
- **"Mulungu Atate"** kutanthauza ubale umene okhulupilira ali anwo ndi iye monga banja. Yohane 6:27; 1 Akorinto 8:6; 15:24; Agalatiya 1:1; Aefeso 5:20; 6:23; Afilipi 2:11; Akolose 1:3; 3:17; 1 Atesalonika 1:1; 2 Atesalonika 1:2; 1 Timoteo 1:2; Tito 1:4; 1 Petro 1:2; 2 Petro 1:17; 2 Yohane 1:3; Yuda 1:1
- **"Mulungu wakundibwezera chilango ine"** kutanthauza kuti amalanga amene alakwira nzake. 2 Samueli 22:48; Masalmo 18:47
- **"Mulungu wa chipiliro ndi chilimbikitso"** kutanthauza kuti ndi Mulungu amene amalimbikitsa omukhulupilira mu nthawi yovuta. Aroma 15:5
- **"Mulungu woleka choipacho"** izi zikutanthauza kuti Mulungu akhoza kuchotsa chilango pa mtundu wa anthu. Yona 4:2
- **"Mulungu openya"** izi zikusonyeza chidwi chake pa anthu. Genesis 16:13
- **"Othandiza amasiye"** kutanthauza chithandizo chake kwa amasiye. Masalmo 10:14
- **"Iye amene amatonthoza iwe"** kutanthauza kuthekera kwake kochotsa zowawa. Yesaya 51:12
- **"Amene amamuuza munthu zoganiza zake"** izi zikutanthauza vumbulutso la zomwe iye akufuna kwa munthu. Amosi 4:13
- **"Iye amene akonza mitima ya iwo onse"** izi zikutanthauza mphamvu zake zakulenga ziwalo za m'kati mwa munthu. Masalmo 33:15
- **"Iye amene angathe kuchita koposa posatu zonse zimene tizipempha kapena tiziganizira monga mwa mphamvu yakuchita mwa ife"** izi zikusonyeza kuthekera kwa zintchito zake. Aefeso 3:20
- **"Amene anaukitsa Yesu kwa akufa"** izi zikuonetsa ntchito yake pa kuuka kwa mbuye Yesu. Aroma 8:11

- **“Atate woyera”** izi zikutanthauza kuyera kwake. Yohane 17:11
- **“Woyera pakati pako”** izi zikutanthauza kuyera kwake. Hoseya 11:9
- **“Mamuna wako”** izi zikutanthauza chikondi chimene amapereka kwa zolengedwa zake. Yesaya 54:5
- **“Woweluza wa akazi wa amasiye”** izi zikutanthauza kukhuzidwa kwake ndi amene alibe owateteza. Masalmo 68:5
- **“Oweluza wa dziko lonse lapansi”** izi zikusonyeza kuti ufumu wake ndi wa dziko lonse lapansi. Genesis 18:25
- **“Mfumu ya kumwamba”** izi zikuonetsa malo a ufumu wake. Danieli 4:37
- **“Tate wa moyo”** izi zikusonyeza umoyo wake. Yohane 6:57
- **“MBUYE”** kutanthauza kuti ndi mfumu ya mafumu. Luka 2:29
- **“AMBUYE ndi mbendera yanga”** kusonyeza kuti ndi iye amene tiyenera kukhala naye chidwi, ngati mbendera ya dziko. Eksodo 17:15
- **“MBUYE ndi tanthwe langa”** kusonyeza kukhazikika kwake kwa omukhulupilira. Masalmo 19:14; 28:1; 144:1
- **“MBUYE wa dziko lonse lapansi”** kusonyeza kuti malo onse a dziko lapansi ali m’manja mwake. Yoswa 3:11, 13; Masalmo 97:5; Mika 4:13; Zekariya 4:14
- **“MBUYE wa kumwamba ndi dziko lapansi”** izi zikutaunthauza kuti kumwamba ndi dziko lapansi zili m’manja mwake. Mateyu 11:25; Luka 10:21; Machitidwe 17:24
- **“MBUYE wa mafumu”** izi zikuonetsa ufumu wake kwa mafumu a dziko lapansi. Danieli 2:47
- **“MBUYE otilenga ife”** izi kusonyeza kagwiritsidwe ntchito ka mphamvu zake nkulenga munthu. Masalmo 95:6
- **“MBUYE chishango chathu”** izi zikutanthauza kuthekera kwake koteteza anthu ake. Masalmo 59:11.
- **“MBUYE ochilitsa iwe”** izi zikuonetsa mphamvu zake zochiza matenda. Eksodo 15:26
- **“MBUYE wakupatula iwe”** izi zikuonetsa mphamvu zake zakusiyanitsa anthu ake ndi dziko lapansi. Eksodo 31:13; Levitiko 20:8; 22:32
- **“MBUYE wakukantha”** izi zikusonyeza chilango chimene Mulungu amapereka kwa anthu. Ezekieli 7:9
- **“AMBUYE opereka”** kusonyeza kuti amawapatsa anthu ake. Genesis 22:14
- **“Mlengi wako”** kutanthauza ntchito imene Mulungu anaigwira pakulenga iwe. Yesaya 54:5
- **“Mlengi wa zinthu zonse”** kusonyeza kuti zonse tiziona analenga ndiye. Mlaliki 11:5; Yeremiya 10:16; 51:19
- **“Mfumu yakumwamba”** kuonetsa chitsanzo chimene iye amaonetsa kwa ena amene ali ndi mphamvu ya ulamuliro. Akolose 4:1
- **“Mboni yanga”** kusonyeza kuti amatiteteza ife. Yobu 16:19
- **“Kulimbika mtima kwanga”** kutanthauza chilengedwe cha munthu pa kudalira Mulungu. Masalomo 71:5
- **“Thandizo langa”** kutanthauza kuti Mulungu amatipulumutsa. Eksodo 18:4; Masalmo 27:9; 40:17; 54:4; 63:7; 70:5; 118:7; 121:1; Ahebri 13:6
- **“Mobisalira mwanga”** kusonyeza kuti munthu amafuna chitetezo cha Mulungu. Masalmo 32:7
- **“Chiyembekezo changa”** kutanthauza chikhalidwe cha munthu pomukhulupilira Mulungu pokhudza tsogolo lake. Masalmo 25:5, 21; 39:7; 62:5; 71:5; 119:74, 81, 114, 147; Machitidwe 23:6; 26:6
- **“Kuwala kwanga”** kutanthauza chikhalidwe cha munthu nchofuna kusogololedwa ndi Mulungu. Masalmo 27:1; Mika 7:8
- **“Pothawirapo ine tsiku la msautso wanga”** kutanthauza chitetezo chake pa nthawi ya mavuto. Yeremiya 17:17; Masalmo 59:16
- **“Mchirikizo wanga”** kutanthauza zabwino zonse zimene iya amatipangira ife. 2 Samueli 22:19; Masalmo 18:18
- **“Amene amafafaniza zolakwa zako”** kutanthauzira chikhalidwe chake chokhululuka machimo. Yesaya 43:25
- **“Mokhalamo mwathu”** kutanthauza kuti iyeyo ndimokhalamo mwathu. Masalmo 90:1
- **“Oweluza wathu”** kutanthauza kuti ndi oweluza wa anthu onse. 1 Samueli 24:15; Yesaya 33:22
- **“Wotipatsa Malamulo”** kutanthauza kuti ndi olamula kwa anthu onse. Yesaya 33:22
- **“Mombolo wathu”** kutanthauza kuti anapereka chipulumutso kwa anthu onse. Yesaya 47:4; 63:16

- **“Mulungu ndiye pothawirapo pathu ndi mphamvu zathu”** kutanthauza kuti ndi chishango kwa anthu onse. Masalmo 46:1
- **“Mwini kumwamba ndi dziko lapansi”** kutanthauza kuti ndi mwini zonse. Genesis 14:19, 22
- **“Muumbi”** kutanthauza kuti amakonza chilichonse ndi manja ake. Yesaya 29:16; 45:9; 64:8; Yeremiya 18:4, 6; Zekariya 11:13; Aroma 9:21
- **“Moombolo wako”** kutanthauza kuti anapereka chipulumutso kwa ine. Yesaya 54:5
- **“Pothawirapo pa anthu ake”** kutanthauza chitetezo chimene iye amawapatsa anthu ake. Yoweli 3:16
- **“Pobisalirapo chimphepo”** kutanthauza chitetezo chimene iye amapereka kwa anthu ake kuwatetza kwa anthu oipa. Yesaya 25:4
- **“Atate wolungama”** kusonyeza chikhalidwe chake. Yohane 17:25
- **“Oweluza olungama”** kutanthauza chigamuro chake chosakondera. Masalmo 7:11; Yeremiya 11:20; 2 Timoteo 4:8
- **“Thanthwe lothawirapo ine”** kutanthauza kukhazikika kwa chitetezo chake. Masalmo 94:22
- **“Thanthwe la mphamvu yanga”** kutanthauza kuti amapereka mphamvu zathu. Masalmo 62:7
- **“Thanthwe la chipulumutso chathu”** kutanthauza kukhazikika kwa chipulumutso chathu. Masalmo 95:1
- **“Malo opatulika”** kutanthauza kuti iye ndi malo okhala. Yesaya 8:14; Ezekiel 11:16
- **“Mphamvu ya chipulumutso”** kutanthauza kluti iye ndipothawirapo. Masalmo 28:8
- **“Pobisalirapo chimphepo”** kutanthauza kuti amapereka pa nthawi ya mavuto. Yesaya 25:4
- **“Mphamvu”** imene imaonetsa phamvu zimene iye amapereka. Yesaya 28:6
- **“Mphamvu ya mtima wanga”** kutanthauza mphamvu zimene iye amapereka kwa omukhulupilira. Masalmo 73:26
- **“Mphamvu za chipulumutso changa”** kutanthauza mphamvu kumbali kwa chipulumutso chathu. Masalmo 140:7
- **“Chitetezo kwa ozunzidwa”** izi zikusonyeza chitetezo chake kwa anthu amene akuzunzidwa ndi anzawo. Masalmo 9:9
- **“Chitetezo pa nthawi ya mavuto”** izi zikutanthauza chitetezo chake pa nthawi ya mavuto. Masalmo 9:9
- **“Othandizira mzimu wanga”** kutanthauza chilengedwe cha munthu polandira umoyo wa uzimu. Masalmo 54:4
- **“Mphunzitsi”** kutanthauza kuthekera kwake kophunzitsa anthu. Yobu 36:22; Yesaya 30:20
- **“Amene amamva mapemphero”** kutanthauza kuti amamva zofuna za anthu onse. Masalmo 65:2
- **“Wakusunga chipangano ndi chifundo”** kutanthauza kuti amasunga mapangano chifukwa cha chikondi. 1 Mafumu 8:23; 2 Mbiri 6:14
- **“Thandizo lopezekeratu m’masautso”** kutanthauza kuti amapezeka kwa ife tikafuna chithandizo. Masalmo 46 :1

Zoyenera kuchita aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Mutu 5, Gawo 3

1. **Mawu a Mlowammalo wa dzina ngati: ‘zanga,’ ‘chako,’ ‘chake’ akagwiritsidwa ntchito pa Maina Mulungu. Kodi zitanthauzanji?**

2. **Pamene a lowammalo a dzina ‘zathu,’ ‘zawo,’ ‘zako’ agwiritsidwa ntchito pa maina a Mulungu, Kodi ndi ubale wanji womwe ukuonetseredwa apa?**

3. **Tengani malongosoledwe osiyanasiyana a Umunthu wa Atate amene alembedwa ku ‘B’ Ndipo fananizani ndi ntchito zake pansipa. Lembani yankho limodzi (monga a, b, kapena c)...**
   a. Mphamvu yonse
   b. Chilungamo
   c. Oona mtima
   d. Chikondi
   e. Moyo wamuyaya
   f. Wa mphamvu zonse
   g. Wopezeka paliponse

h. Wodziwa zonse
i. Wosasintha sintha
j. Choonadi

4. Tengani ntchito za Atate zimene zalembedwa mu gawo 'D' ndipo muzifanizire pa ntchito za Atate musimu. Lembani yankho limodzi a, b, c

a. Ulamuliro
b. Mlengi
c. Mtetezi
d. Chitsanzo
e. Wopatsa
f. Woweruza
g. Mtsogoleri
h. Wokonda
i. Wopereka
j. Wokhazikitsa

Gawo 4
Mulungu Mwana (Chiphunzitso cha Khristu-Christology)

A. Umunthu wa Yesu Khristu

Yesu Khristu, mwana, ndi Mulungu mu thupi. Si munthu wabwino amene anakhara mulungu, koma Mulungu amene anakhara munthu (Yohane 1:1, 14). Iyeyo ali ndi chikhalidwe chenicheni cha Mulungu (Yohane 14:8-9; Ahebri 1:3).

1. Kukhala Kwake Asanabadwe

Yesu analipo asanabadwe ngati munthu. Tinaudzidwa kuti ***"pakuti mwa iye, zinalengedwa zonse zam'wamba ndi dziko lapansi, zooneka ndi zosaoneka kapena mipando yachifumu kapena maufumu, kapena maukulu kapena maulamuliro zinthu zonse zinalengedwa mwa iye ndi kwa iye"*** (Akolose 1:16). Yesu mwwini anawauza a yuda kuti ***"Abraham asanabadwe ine ndilipo"*** (Yohane 8:58). Uthenga wa Yohane umafotokoza kukhalapo kwake asanabadwe.

Yohane amatsegulira ndi kuti ***"Pachiyambi panali mau,ndipo mau anali kwa Mulungu,ndipo mau ndiye Mulungu.Zonse zinalengedwa ndi iye;ndipo kopanda iye sikunakhala kanthu kali konse kolengedwa"*** (Yohane 1:1-3). Kupitiliza bukuli, Yohane anati, ***"ndipo mau anasandulika thupi, nakhazikika pakati pa ife, ndipo nawadalitsa"*** (Yohane 1:14).

2. Mgwirizano wa Mulungu ndi Munthu

Yesu ndi Mulungu komanso munthu. Ndi Mulungu okwanira komanso munthu okwanira. Chilungamo ichi ndi chovuta kuchimvetsa komabe ndi chilungamo.

Yesu anawafunsa fuso afarisi atasara pang'ono kuti aphedwe pa mtanda (Mateyu 22:41-46). Anafunsa nati "Khristu akhala bwanji mbuye wa Davide komanso Mwana wake?" Kuti izi zitheke nkuti Khristu ali Mulungu komanso munthu.

3. Ubwino Wake

Yesu anali wabwino munjira iliyonse. Ngati Mulungu anali wabwino, koma ena akafunsa ubwino wa umoyo wake ngati munthu.

Timaphunzura ubwino wake mu buku la Aroma kuti ***"monga uchimo unalowa dziko lapansi mwa munthu m'modzi, ndi imfa mwa uchimo; chotero imfa inafikira anthu onse, chifukwa kuti onsewo anachimwa"*** (Aroma 5:12). Munthu m'modziyo ndi Adamu yemwe kugwa kwake kunafaritsa uchimo ndi imfa kwa anthu onse (Aroma 5:13-19). Yesu analibe bambo ake a kuthupi koma kuti bambo ake anali Mzimu Woyera (Luka 1:35). Izi sizinachitike chonchi kuti angotchulidwa "Mwana wa Mulungu" koma kuti tchimo ndi imfa zimene zinachokera kwa mamuna oyamba, Adamu zisadutse kwa iye. Kusiyana ndi anthu ena onse Yesu Khristu analibe uchimo wa Adamu. Pamene Adamu analengedwa bwinobwino koma anachimwa, Yesu analengedwa wabwino ndipo sanachimwe.

Mau a Mulungu amatiuza kuti Yesu anakhara moyo wabwino ndipo mpaka kale adzakhala wabwino. Sanachite tchimo lililonse kapena kuyankhula za chinyengo (1 Petro 2:22). Chifukwa cha kusachimwa kwake ali kuthupi, kusonyeza kuti adzakhala wabwino mpaka kale (Ahebri 5:9; 7:28) kutanthauza kuti sangachimwe.

B. Ntchito za Yesu Khristu

Ntchito ya Yesu Khristu mu dongosolo la Mulungu inali kuchita zomwe dongosolo limamuuza kuti achite (Yohane 8:28-29). Anamaliza ntchitoyo yomwe inali kudzipereka iye kuti akafere anthu pamtanda kuti anthu apulumutsidwe (2 Akorinto 5:21).

1. Kufika Nkwa Yesu Ngati Mwana

Kubadwa kwa Yesu Khristu kunaneneledwa mu chipangano chakale, makamaka kudzera mwa m'neneri Yesaya (Yesaya 7:14; 9:6; 11:1; 53:2). Yesu ndi "mbeu ya mzimayi yolonjezedwa" (Genesis 3:15) kunaneneledwa kuti adzabadwira ku Betelehemu (Mika 5:2) ndipo adzakhala mbeu ya Abrahamu. (Genesis 22:18; Mateyu 1:1; Agalatiya 3:16), kudzera kwa Isaki (Genesis 21:12), Yakobo (Genesis 35:10-12), Yuda (Genesis 49:8-11) Jese (Yesaya 11:1) ndi Davide (2 Samueli 7:12-16; Yeremiya 23:5; Masalmo 132:11).

2. Kubadwa mwa Namwaliyo

Dongosolo la Mulungu linafuna kuti Yesu mpulumutsiyo (Khristu) abadwire mwa namwaliyo (Yesaya 7:14). Ngakhale izi zili zofunika ku phunziro la buku loyera, ndizofunikanso kudziwa kuti kubadwa kwa Yesu kunali kodabwisa. Chinenero chimenechi chinakwaniritsidwa kudzera mwa Maliya (Mateyu 1:20, 25).

3. **Kufa kwa Khristu**

Imfa ya Yesu inakwaniritsa zinthu zambiri. Sanali oyenera kuti afe (Luka 23:4). Onse amene anachimwa (Aroma 3:23) ndi amene anayenera kufa (Aroma 6:23). Chifukwa choti tonse tinachimwa tiyenera kufa. Yesu sanayenera kufa chifukwa sanachimwe, koma anasankha kutifera ife chifukwa cha zochimwa zathu pamaso pa Mulungu woyera ndi wolungama (Yohane 10:15-17).

a. **Kulowam'malo mwa wina**

"Kulowa "m'malo mwa wina" kukutanthauza kuti Yesu anatenga malo athu potifera pa mtanda. Tinauzidwa kuti, ***"iye anasenza machimo athu mwini yekha m'thupi mwache pamtanda, kuti ife titafa kumachimo tikhale ndi moyo kutsata chilungamo; ameneyo mikwingwirima yake munachilitsidwa nayo"*** (1 Petro 2:24). Yesu sanangofera pamtanda paja chifukwa chaife, koma m'malo mwa ife ku "tembelero" lathu (Agalatiya 3:13).

b. **Chiwombolo**

"Chiwombolo" kukutanthauza kuti munthu anapulumuka chifukwa cha kudzipereka kwake. Izi zikuonetsa ukapolo umene unakhalapo pofuna kutigulira ufulu wathu. Chipulumutso kumachimo chikutanthauza kukhulukidwa kwa machimo zomwe zinatichotsa mu ulamuliro wa Satana nkutipititsa mu ufumu wa Mulungu (Akolose 1:13 -14).

Yesu analipira mtengo waukulu chifukwa cha anthu onse (2 Petro 2:1) kuti onse amasulidwe mu uchimo ndi imfa (Aroma 8:2). Mtengowu unali mwazi wake kutanthauza imfa ya pamtanda (Chivumbulutso 5:9-10). Chifukwa choti mtengo wa ufulu wathu unaperekedwa, ndifeno omasuka kusankha kulambira mbuye (1 Akorinto 6:19-20) kuthokoza chisomo chimene anatichitira osati chifukwa cha chilamulo. Tiyenera kukhala akapolo okhazikika (amene amaziikiza kwa mfumu mmodzi chifukwa cha ubwino wa mfumuyo) kwa Khristu koyamba osati zoganiza za munthu (1 Akorinto 7:19-23).

Tiyenera kumenyabe zolimba kuti tikhalebe ndi ufulu umene Khristu anatipatsa (Agalatiya 5:1). Muchikhalidwe chathu cha umunthu timalolera mayesero komanso machimo amene amaika mzimu wathu mu ukapolo umene umatipangitsa kukhala ngati osakhulupilira (Aefeso 5:1-14). Ufulu umene Yesu Khristu anapereka mwa chisomo kwa ife siziyenera kugwiritsidwa ntchito ngati "mwayi wa thupi" koma chikondi pamene tikutumikira wina ndi nzake.

c. **Chiyanjano**

"Kuyanjanitsa" ndi kuchotsa udani pakati pa magulu awiri. Chotsatira cha kuyanjana ndi mtendere.

Osakhulupilira amatchulidwa kuti "adani a Mulungu" (Aroma 5:10) ndipo akukumana ndi mkwiyo wake (Aroma 5:9). Izi zikutanthauza kuti munthu aliyense amene samakhulupilira Yesu Khristu kuti ndi mpulumutsi (Yohane 3:16, 18, 36), ali ndi mkwiyo wa Mulungu (Aefeso 2:3). Yesu anabwera kuzayanjanitsa a yuda ndi amitundu onse ndi Mulungu kuti pakhale mtendere (Aefeso 2:16) kupereka chiyanjanitsocho popereka thupi lake (Akolose 1:22).

Machimo anayenera kulipilidwa ndicholinga chakuti tiyanjane ndi Mulungu (2 Akorinto 5:19). Koma Yesu anatiyanjanitsa mwa Khristu Yesu ndikutipatsa utumiki wa chiyanjano pakati pa anthu (2 Akotinto 5:18:21). Tchimo limayenera kulipidwa kuti tiyanjane ndi Mulungu (2 Akorinto 5:18-21). Utumiki wa chiyanjano pa munthu ndi pamene wina wakhala obweretsa mtendere pakati pa anthu awiri kapena ambiri amene ali pa udani (Mateyu 5:9).

Chifukwa choti tinayanjanitsidwa ndi Mulungu zikuonetsa ubwino ndi ukulu wa chikondi chake (Aroma 5:8; Luka 6:31-35). Chiyanjanochi ndi cha munthu aliyense (Akolose 1:20).

d. **Kukwaniritsa**

"Kukwaniritsa" kukutanthauza kukwanilitsa kulungama komanso chilungamo cha Mulungu woyera.Izi zimachitika kudzera munjira yopereka nsembe.

Mulungu amakwiya ndi machimo. Mkwiyo wake umaphunzitsidwa ku chipangano chakale komanso chatsopano (Deutronomo 6:14-15; Yoswa 23:16; Masalmo 78:21; Yohane 3:36; Aroma 1:18; Aefeso 2:3; 1 Atesalonika 2:16 ndi ena ambiri). Komanso Mulungu ndi wa chikondi ndi chifundo. Monga Charles Ryrie anati,

> Ndiye tisatenge chipangano chakale ngati kuti chinachokera kwa fano lomwe lisali Mulungu wabwino yemwe amafuna kusangalasidwa kapena kukwaniritsidwa, koma kwa Mulungu olungama amene samayang'anira tchimo koma amene chikondi chake chimatipatsa ife njira yoyanjanirana naye mwini.[99]

Mkwiyo wa Mulungu, ndiyeno umayenera kuti uchotsedwe ndipo imfa ya Yesu Khristu ndi imene inachotsa mkwiyo wa Mulungu pokhuza machimo (Aroma 3:23-25). Anaombora mkwiyo wa Mulungu kwa anthu onse (1 Yohane 2:2) poonetsa chikondi chake (1 Yohane 4:10). Ili linali gawo la chikonzero cha Mulungu ndipo linali gawo lofunikira pa chifukwa chimene Yesu anakhalira munthu (Ahebri 22:17-18).

4. Kuuka kwa Ambuye Yesu

"Kuuka" ndi mau amene amagwiritsidwa ntchito polongosola munthu amene wauka kwa kufa mu thupi losabvunda lomwe silingazafenso (1 Akorinto 15:42, 54). Timasiyanitsa ndi "kudzuka" komwe kumatanthauza munthu amene wadzuka kwa kufa ndi thupi lomwe lingazavunde kutanthauza kuti likhoza kuzafanso (1 Mafumu 17:21-22; 2 Mafumu 4:34-35; Yohane 11:43).

Yesu Khristu anaukitsidwa kwa akufa. Malemba amanena momveka bwino kuti Yesu Khristu anamwaliradi osati kugona kapena kukomoka (Mateyu 27:62-66; Marko 15:39, 44; Luka 23:48, 49; Yohane 19:33). Manda anaperekedwa kuti akwaniritse ulosi (Yesaya 53:9; Mateyu 27:57-58; Marko 15:42-45; Luka 23:50-52; Yohane 19:38), ndipo Yesu anakulungidwa mu nsalu yokutira anthu akufa (Mateyu 27:59-60; Marko15:46; Luka 23:53-54; Yohane 19:40-42) naikidwa m'manda (Mateyu 27:62-66). Ngakhale ayuda amadziwa kumene iye anaikidwa, ndipo anaikapo azilonda anai a chiroma polowera pake ndikuikapo chizindikiro pamandapo (Mateyu 27:62-66). Kenako a yudawo anafalitsa mphekesera yonena kuti ophunzira a Yesu aba thupi la yesulo (Mateyu 28:11-15; Marko 14:15).

Pa tsiku la chitatu mwala unakankhilidwira pa phiri (Mateyu 27:60 anagwiritsa ntchito mau a chi Greek KULIO kutanthauza kuti kusunthidwa), (Marko 16:3-4 anagwiritasa ntchito ANAKULIO kutanthauza kuti kukankhilidwira m'mwamba), (Luka 24:2 anagwiritsa ntchito APOKULIO kutanthauza kuti unakankhlidwa kutali; ndipo Yohane 20:1 anagwiritsa AIRO kutanthauza kuti "kukweza m'mwamba." Mwalawo unakankhilidwira ku phiri kenako "ndikukwezedwa m'mwamba" ndipo m'mandamo munalibe kanthu (Mateyu 28:5-8; Marko 16:2-8; Luka 24:1-8; Yohane 20:1).

Zomwe zinasala m'mandamo zinali zovara zimene anakuta thupi lake. Zinakonzedwa munjira yonena kuti thupilo silinabedwe, koma kunachitika cha uzimu (Yohane 20:2-10).Yesu Khristu anakutidwa mu nsalu za bafuta. Mlezi umene unali pamutu pake ndi umene panalibe kusonyeza kuti thupi linali litapita. Sizikanakhala kotheka kuti munthu angataitse nthawi yake nkumasura thupilo mu nsaluzo nkulichotsamo ndikubwezeretsa momwe nsaluzo zinalili.Thupilo linazichotsamo lokha.

Atauka kwa akufa, Yesu anaonekera kwa Maliya magadala (Yohane 20:14), kwa azimayi ena (Mateyu 28:9-10), kwa Petro (Luka 24:34; 1 Akorinto 15:5), kwa omusatira ake awiri pa njira yak u Emau (Luka 24:13 -33), kwa ophunzira ake koma popanda Tomasi (Luka 24:36-43; Yohane 20:19-24) komanso kachiwiri iye alipo (Yohane 20:26-29), kwa omutsatira ake asanu ndi awiri pa Nyanja ya Galileya (Yohane 21:1-23), kwa abale oposa mazana asanu pa phiri ku Galileya (1 Akorinto 15:6), kwa mchimwene wake Yakobo (1 Akorinto 15:7), kwa ophunzira ake khumi ndi m'modzi m'mene iye amakwera kumwamba (Mateyu 28:16-20; Luka 24:33-52; Machitidwe 1:3-12); ndipo pomaliza anaonkeranso kwa Paulo atakwera kale mmwamba (Machitidwe 9:3-6; 1 Akorinto 15:8).

Kuuka kwa Yesu ndikofunikira kutengera mu uthenga wabwino wa Yesu Khristu (1 Akorinto 15:1-3). Kumasiyanitsa iye ndi atsogoleri a dziko lapansi azipembezo amene palibe mwa iwo anaukitsidwapo.

Yesu mwini analankhura kuti adzauka kwa akufa (Mateyu 16:21; 17:9, 22-23; 20:18-19; 26:32; Marko 9:10; Luka 9:22-27). Ndipo akanakhala kuti sanauke kwa akufa, utumiki wake sukanakhulupilidwa ndipo bwenzi tidakali mu uchimo wathu (1 Akorinto 15:16-17).

Mulungu Atate ndi amene anamuukitsa iye (Akolose 2:12; 1 Atesalonika 1:10; 1 Petro 1:21; Ahebri 13:20), komanso Mzimu Woyera (Machitidwe 2:24; Aroma 8:11; 1 Petro 3:18).

Kuuka kwa Yesu Khristu ndi umboni wachilungamo choti zonse zimene iye ananena ndi kuchita zinali zowona ndi zabwino.

Kuvomereza kuuka kwa ambuye Yesu ndi pamene pagona moyo wathu wa Chikhristu (Aroma 6:4).

5. Kukwera M'mwamba kwa Yesu Khristu

Kukwera m'mwamba kwa Yesu Khristu kukutanthauza kubwelera kwake kumwamba kuchokera pa dziko lapansi ataukitsidwa kwa akufa. Anatenga mpando wake ku dzanja lamanja la Mulungu Atate wa mphamvu zonse, udindo wa pamwamba kudzachilengedwe zonse (Masalmo 110:1; Aefeso 1:20; Akolose 3:1; Ahebri 1:3, 13; 8:1; 10:12; 1 Petro 3:22).

Kukwera kumwamba kwake kunachitika patasara masiku khumi kuti Pentekoste ichitike. Kenako anatumiza Mzimu Woyera (Machitidwe 2:33) monga iye analonjezera (Yohane 14:16-17) ndikukonza mpingo wake (Machitidwe 1:9-11 cf. Machitidwe 2). Kukwera kwake kumwamba ndi umboni wonena kuti ndi wamkulu kuposa Angelo (Ahebri 1:3-13).

Pamene Yesu anakwera kumwamba, anatenganso mizimu ya amene anamwalira nakaika ku "chifuwa cha Abrahamu" (Luka 16:22; Aefeso 4:7-10). "Anaperekanso mphatso kwa athu" (Aefeso 4:8) zomwe zinagawidwa ndi Mzimu Woyera ku mpingo (1 Akorinto 12:11).

C. Nthawi ya Yesu Khristu

Nthawi imene Yesu amakhala ku dzanja lamanja la Mulungu Atate kufikira atadzabwera pa dziko lapansi imatchulidwa kuti "nthawi". Ndizofunikira kwa iye mudongosolo la Mulungu kuti adzikhala pa dzanja la manja la Mulungu Atate kufikira atadzabweranso pa dziko la pansi pa chigonjetso chomaliza pamene ***"adani ake"*** adzakhala chopondapo mapazi ake (Masalmo 110:1).

Nthawi imatanthauza mpando olemekezeka ngati okwera kumwamba komanso oyenera matamando Mulungu-munthu. Ndi chithunzi chonena kuti ***"mphamvu zonse zaperekedwa kwa iye,"*** komanso kuti ***"pa dzina lake bondo lililonse ligwade"*** (Afilipi 2:9-10). Ndikukwanilitsa ulosi wa Danieli 7:13-14.

Nthawiyi Yesu amatumikira munthu ngati:

1. Wopembezera

Monga "wopembezera" Yesu Khristu amapemphelera kwa Atate oyera mtima onse (Ahebri 7:25). Izi amachita limodzi ndi Mzimu Woyera (Aroma 8:26, 27, 34) ndipo ndi pempho kwa Atate kuti amene akonda Mulungu zinthu zonse zithandizane kuwachitira ubwino (Aroma 8:28) monga kutsimikiza kwa mtima wake.

2. Nthandizi

Monga nthandizi wathu, Yesu amaimira ngati wachitetezo amene amayankha milandu yobweresedwa ndi Satana pofuna kulimbana ndi anthu a Mulungu (Yohane 2:1; Chivumbulutso 12:10).

3. Nkhala Pakati

Monga nkhala pakati wathu, Yesu ndi "munthu okhala pakati wathu" amene amatilumikiza ndi Mulungu. Nkhala pakati ndi amene wasankhidwa kuti ayanjanitse magulu amene sakugwirizana kapena amene akufuna kuyanjana.

Yesu Khristu ndi "nkhalapakati" pakati pa Mulungu ndi munthu (1 Timoteo 2:5). Mu udindo wake, anayanjanitsa chipangano chatsopano pakati pa Mulungu ndi munthu chimene chinakhazikika mu chikondi osati chilamulo (Ahebri 8:6-13). Chipangano chatsopano chinabwera chifukwa cha nsembe yomwe anapereka chifukwa cha uchimo, polipira chilango chauchimo wochitika pansi pa chipangano chakale kusatira malamulo a Mose (Ahebri 9:13-15). Chipangano chatsopanochi chizakhala mpaka kalekale (Ahebri 12:22-24).

Yesu ananena yekha kuti iye anali nkhalapakati wa Mulungu ndi munthu pamene ananena kuti ***"palibe angadze kwa Atate koma mwa ine"*** (Yohane 14:6).

4. Wansembe Wamkulu

Khristu ndi wa "nsembe wamkulu" kuchokera kusankhidwa ndi Atate. Sanabadwe mu banja la a nsembe la Levi kotero kuti sakanatenga udindo wa ansembe kutengera kumene anabadwira (Ahebri 5:4-10; 7:5-28). Ukulu wa nsembe wa Yesu Khristu ndi mutu wa ukulu wa bukula Ahebri.

Yesu ndi wa nsembe wamkulu ngati Melikizedeke, amene anakhalapo zaka mazana anai unsembe wa Levi usanayambike mu nthawi ya Abrahamu (Ahebri 7:1-3). Kotero kudamuyenera kufanizidwa ndi abale m'zonse kuti akazakhala wa nsembe wa chifundo ndi wokhulupilika m'zinthu za kwa Mulungu kuti apereke dipo la zoipa za anthu (Ahebri 2:17; 4:14-15). Unsembe wake ndi wosatha (Ahebri 6:20; 7:3, 24).

Ntchito ya wansembe ndi kupereka nsembe (Ahebri 8:1-3). Yesu Khristu anadzipereka yekha (Ahebri 9:6-14) ngati "Nsembe imodzi ya nthawi zonse" (Ahebri 10:10, 12). Unkhoswe wake ndi ukhala pakati wake ndiyeno ndikutambasura ukulu wansembe wake.

Chifukwa chakuti mipingo yonse ndi ya a nsembe (1 Petro 2:5, 9; Chivumbulutso 1:6), tiyenera tisatizire Yesu Khristu (1 Akorinto 11:1) pozipereka tokha ngati nsembe pa zofuna za Mulungu (Aroma 12:1).

5. **Mutu wa Mpingo**
Yesu Khristu ndi "mutu" kapena msogoleri wa mpingo (Aefeso 1:22-23; Afilipi 1:18). Amene amakhulupilira Yesu amapanga thupi la Khristu lomwe limatchulidwa kuti mpingo (1 Akorinto 12:13).

Yesu ndimamuna olonjezedwa wa mpingo (Aefeso 5:23) ndipo chifukwa cha ichi amachulukitsa mopitiliza chikondi chake chosasintha (Aefeso 5:25-27). Mwambo weniweni wa ukwati ukachitikira kumwamba Yesu Khristu asanabwerenso kachiwiri (Chivumbulutso 19:7-10 cf.11-16) koma chikondi ndi kukhulupilika kulipo pano. Mpingo ngati mkwatibwi ukukonzedwa kukonzekera mamuna wake (Aefeso 4:15; 5:26-27).

6. **M'busa**
Mau oti "mtumikii" ndi mau amene amatanthauza kuti "M'busa". Khristu monga "m'busa wabwino" anapereka moyo wake chifukwa cha nkhosa zake (Yohane 10:11) zomwe zinamupangisa kuti iye akhale "wansembe" wopambana (Ahebri 13:20).

Nthawi yake kudzanja la manja la Mulungu Atate wa mphamvu zonse, iyeyo ndi "wamkulu wa abusa" (1 Petro 5:4), amene amasogolera ndi kuteteza nkhosa zake.

D. Mmene tingamulongosolele Yesu Khristu

- **"Nkhoswe"** kusonyeza kuti amayankhura ndi Atate potiteteza. 1 Yohane 2:1
- **"Oyamba ndi otsiliza"** ndi chilembo choyamba ndi chotsiliza mu afabeti ya chi Greek zomwe zikutanthauza kuti ndi maziko a ubale, kapena chiyanjano. Chivumbulutso 1:8; 21:6; 22:13
- **"Amen"** kutanthauza kuti ndi mau otsiliza mu phinziro lililonse. 2 Akorinto 1:20; Chivumbulutso 3:14
- **"Ozozedwa"** zomwe zikukamba za kusankhidwa kwake kosatha ngati mpulumutsi. 1 Samueli 2:35; 2 Mbiri 6:42; Masalmo 2:2; 28:8; 84:9; 89:38, 51; 132:10, 17; Danieli 9:28; Machitidwe 4:26
- **"Mtumwi"** zomwe zikusonyeza kuti anatumidwa ndi ulamuliro. Ahebri 3:1
- **"Olemba ndi okhazikitsa chikhulupiliro chathu"** kutanthauza kuti ngati Mulungu, Khristu analemba dongosolo ndipo ngati munthu anakwaniritsa. Ahebri 12:2
- **"Olemba chipulumutso"** kutanthauza ntchito yake monga chiyambi cha chipulumutso. Ahebri 2:10
- **"Chiyambi ndi mathero"** kutanthauza kuti iyeyo ndiofunikira pa moyo. Chivumbulutso 21:6; 22:13
- **"Chiyambi pa chilengedwe cha Mulungu"** kutanthauza kuti iyeyo ndi olamulira chilengedwe cha Mulungu. Chivumbulutso 3:14
- **"Odalitsidwa ndi opambana"** kusonyeza udindo wake wa ulamuliro woposa onse. 1 Timoteo 6:15
- **"Gawo la ambuye"** kutanthauza kutenga kwa umunthu wake kuchokera ku ufumu wake. Yesaya 4:2
- **"M'kate wa Mulungu"** kutanthauza kusunga kwake kwa moyo. Yohane 6:33, 51
- **"Mkate wa moyo"** kutanthauza kuti ndi iye amene amapereka zofuna za moyo. Yohane 6:35, 48
- **"Mkwati"** kutanthauza kukonda ndi kuteteza kwake kwa abale omukhulupilira. Yesaya 62:5; Mateyu 9:15; 25:1, 5, 6, 10; Marko 2:19, 20; Luka 5:34, 35; Yohane 2:9; 3:29; Chivumbulutso 18:23
- **"Nyenyezi yowala m'mawa"** kutanthauza kuti iye ndi nyenyezi yowalitsitsa yomwe yazungulidwa ndi mizimu ya ku midima. Chivumbulutso 22:16
- **"Mkulu wa a busa"** kutanthauza kuti iye ndi amene amayang'anira nkhosa zonse. 1 Petro 5:4
- **"Mwala osankhidwa wa pangodya mwa ulemu"** kutanthauza kuti iye anachita kusankhidwa mwapadera. Mwala wa pangodya umapanga kaonekedwe ka chomangidwa. Aefeso 2:20; 1 Petro 2:4, 6.
- **"Yesu Khristu mbuye wanga" k**utanthauza kuti Yesu Khristu ndi mpulumutsi ndiponso ndi wolamula moyo wanga. Afilipi 3:8
- **"Khristu Yesu chiyembekezo chathu"** kutanthauza kuti Yesu mpulumutsi amakhala chiyembekezo cha tsogolo lathu. 1 Timoteo 1:1
- **"Khristu wa Mulungu"** kutanthauza kusankhidwa kwake ngati mpulumutsi. Luka 9:20; 23:35
- **"Karonga wa khamuro"** kutanthauza udindo wake wa chilamuro kwa a silikali. Danieli 8:11
- **"chitonthozo cha Israeli"** kutanthauza chilimbikitso chimene Khristu amapereka. Luka 2:25
- **"Pangano kwa anthu"** kusonyeza kuti Yesu ndi chiyambi cha chipangano chatsopano kwa okhulupilira iye. Yesaya 42:6
- **"Khomo"** kutanthauza kuti iyeyo ndi polowera ufumu wa Mulungu. Yohane 10:7, 9
- **"Tate wosatha"** kusonyeza kuti iyeyo ndi Mulungu wachikhalire. Yesaya 9:6

- **“Moyo wosatha”** kutiphunzitsa kuti umapezeka kwa munthu, osati chinthu. 1 Yohane 1:2
- **“Thanthwe losatha”** kutiphunzitsa kukhazikika kwake. Yesaya 26:4
- **“Chionetsero chenecheni cha khalidwe lake”** kutanthauza umunthu wa Khristu kukhala Mulungu kuthupi. Ahebri 1:3
- **“Wokhulupilika ndi wachilungamo”** kusonyeza kukhulupirika ndi chilungamo chake. Chivumbulutso 19:11
- **“Wokhulupilika ndi mboni yachilungamo”** kusonyeza kukhulupilika kwake ndi chilungamo pokhuza zochitika mu ulosi. Chivumbulutso 3:14
- **“Mboni yokhulupilika”** kutanthauza umboni wakuuka kwake. Chivumbulutso 1:5
- **“Oyamba ndi otsiliza”** kutsonyeza kuti iyeyo ndi gwero la chilengedwe. Chivumbulutso 1:17; 2:8; 22:13
- **“Oyamba kuuka kwa akufa”** kutsonyeza kuti iye ndiwoyamba kugonjetsa imfa ndipo nkulandira thupi losafa. Akolose 1:18; Chivumbulutso 1:5
- **“Chiyambi cha zolengedwa zonse”** kusonyeza kuti iye ndi chiyambi cha chilengedwe. Akolose 1:15
- **“Chipatso choyamba kwa amene agona”** kutanthauza kuti iyeyo ndi m’dalitso oyamba wa kuuka kwa akufa. 1 Akorinto 15:20
- **“Fungo lonunkhira bwino”** kufuna kutionetsa chikondi chake chomwe anachita potifera ife. Aefeso 5:2
- **“Mnzake wa otolera misonkho ndi anthu ochimwa”** kusonyeza chisamaliro chake kwa amene dziko lawakana komanso ophwanya chilamulo. Mateyu 11:19; Luka 7:34
- **“Ulemelero wa anthu a Israeli”** kutanthauza kuyenera kwake kulandira matamando. Luka 2:32
- **“Mulungu wa dziko lapansi lonse”** kusonyeza kukula kwa mphamvu zake kwa anthu onse. Yesaya 54:5
- **“Mulungu wa pamwamba pa onse”** kutanthauza kuti Mulungu wa Israeli. Aroma 9:5
- **“M’busa wabwino”** kutanthauza chilengedwe cha usogoleri komanso chitetezo chake. Yohane 10:11
- **“Wamkulu wa nsembe opambana”** kutanthauza luso limene ali nalo akakhala pa mpando wake. Ahebri 4:14
- **“Kuwala kopambana”** kutanthauza kuthekera kwake kochotsa m’dima. Yesaya 9:2; Mateyu 4:16
- **“Mbusa wopambana”** kusonyeza ukulu wake wazomwe iye amapereka ndi zomwe iye amateteza. Ahebri 13:20
- **“chikole cha Pangano loposa”** kutanthauza kuti Yesu anali lonjezo la pangano la bwino ndi Mulungu. Ahebri 7:22
- **“Mlonda wa mizimu yathu”** kutanthauza chitetezo chake cha mizimu yo mukhulupilira. 1 Petro 2:25
- **“Msogoleri”** kutanthauza nzeru zake pa usogoleri wake. 1 Akorinto 11:3; Aefeso 4:15; Akolose 2:19
- **“Amene anadzuka nkukalamura amitundu”** kutanthauza ulamuliro wake umene iye ali nao kwa anthu a mitundu. Aroma 15:12
- **“Amene amayeretsa”** kusonyeza kuthekera kwa a mbuye kugwira ntchito yake. Ahebri 2:11
- **“Amene amafufuza maganizo komanso mtima”** kusonyeza kuthekera kwa ambuye kodziwa zoganiza zonse za Mulungu. Chivumbulutso 2:23
- **“Msogoleri wa thupi”** kusonyeza nzeru zake za usogoleri wa mpingo. Akolose 1:18
- **“Msogoleri wa mpingo”** kusonyeza nzeru zake za usogoleri kwa okhulupilira. Aefeso 5:23
- **“Msogoleri wa malamulo ndi chilamulo chonse”** kutanthauza mphamvu ya chilamulo chake. Akolose 2:10
- **“Otenga zonse”** kutanthauza kuti monga Mwana wa Atate, amatenga zinthu zonse. Ahebri 1:2
- **“Wamkulu wa ansembe”** kutionetsa udindo ali nao. Ahebri 22:17; 3:1; 4:14, 15; 5:5, 10; 6:20; 7:26; 8:1; 9:11; 13:11-12
- **“Iye amene amatikonda ife ndipo amatimasura ife ku machimo athu”** kutanthauza kukhulukidwa kwa machimo athu ndi Khristu chifukwa cha chikondi chake. Chivumbulutso 1:5
- **“Mwana wake wobadwa yekha”** kusonyeza kuti Yesu Khristu ndi woposa chilengedwe chonse. Yohane 3:16; Ahebri 11:17; 1 Yohane 4:9
- **“Woyera ndi wolungamayo”** kusonyeza chikhalidwe chake chabwino. Machitidwe 3:14
- **“Woyera wa Mulungu”** kusonyeza moyo wake wabwino umene iye anakhala ali munthu. Marko 1:24; Luka 1:34; Yohane 6:69

- **“Mtumiki woyera”** kusonyeza kuti anaphunzira kulemekeza monga Mwana ayenera kuchitira. Machitidwe 4:27, 30 (mau a chi Greek PAIS anagwiritsidwa ntchito kutanthauza kuti Mwana)
- **“Chiyembekezo cha Israeli”** zomwe zikuonetsa Israeli ngati chiyambi cha chiyembekezo. Yeremiya 14:8; 17:13; Machitidwe 28:20
- **“Nyanja ya chipulumutso”** zomwe zikusonyeza mphamvu zoyenera kubweretsa chipulumutso. Luka 1:69
- **“Fanizo la Mulungu wosaonekayo”** kusonyeza kuti Yesu ndi Mulungu ali mu thupi. Akolose 1:15
- **“Emanuel”** lomwe liri dzina la chi Hebri kutanthauza kuti “Mulungu ali nafe.” Yesaya 7:14; 8:8; Mateyu 1:23
- **“Mphatso yosaneneka”** kutanthauza kuti palibe mau amene angalongosole bwino ubwino wa Yesu. 2 Akorinto 9:15
- **“Yesu wa ku Nazareti”** kutanthauza dera limene Yesu anakulira. Mateyu 26:71; Marko 1:24; 10:47; Luka 4:34; 18:37; 24:19; Yohane 1:45; 18:5, 7; Machitidwe 2:22; 6:14; 10:38; 22:8; 26:9
- **“Woweluza amoyo ndi akufa”** kutanthauza udindo wake umene ali ndi chilamulo chopereka chigamulo ndi chilango. Machitidwe 10:42; 2 Timoteo 4:1
- **“Mfumu ya mafumu”** kutanthauza udindo wake waukulu oposa ma udindo ena onse. Chivumbuluso 19:16
- **“Mfumu ya maiko”** kutanthauza udindo wake waukulu kwa magulu a ndale. Chivumbulutso 15:3
- **“Nkhosa ya Mulungu”** kutanthauza nsembe imene Yesu Khristu anadzipereka yekha kufuna kuonetsa kulungama kwa Mulungu. Yohane 1:29, 36
- **“Adamu wotsiliza”** kutanthauza kuti iye ndi munthu wotsiliza kukhala moyo wopanda ntchimo. 1 Akorinto 15:45
- **“Moyo”** kutanthauza kuti moyo weniweni umapezeka mu umunthu wa Khristu osangoti munthu wamba. Yohane 1:4; 11:25; 14:6
- **“Mzimu wopereka moyo”** zomwe zimagwiritsidwa ntchito pofuna kulongosola mgwirizano wa Yesu ndi Mzimu Woyera. 1 Akorinto 15:45
- **“Kuunika kukhale chivumbulutso kwa anthu a mitundu”** kutanthauza kuti Yesu ndi wa wina aliyense. Luka 2:32
- **“Kuunika kwa moyo**” kutanthauza usogoleri wake pa ulendo wathu umene timakumana ndi zinthu zovuta kuzimvetsa m’moyo. Yobu 33:30; Masalmo 49:19; 56:13; Yohane 8:12
- **“Kuunika kwa anthu”** kutanthauza kutsogolera kwake kopezeka kwa anthu onse. Yohane 1:4
- **“Kuunika kwa dziko”** kutanthauza kutsogolera kwake pa dziko lapansi kuti anthu asayende mu m’dima. Yohane 8:12; 9:5
- **“Wamoyo”** kutanthauza chikhalidwe chake chosatha pa kuukitsidwa kwake. Chivumbulutso 1:17-18
- **“Mwala wamoyo”** kutanthauza kukhazikika kopezeka m’moya mwake. 1 Petro 2:4
- **“Mbuye”** kutanthauza ulamuliro wake. Machitidwe 4:24; Chivumbulutso 6:10
- **“Yesu Khristu mbuye ndi mpulumutsi”** kutanthauza kuti anagwiritsa ntchito ulamuliro wake kupulumutsa anthu ku zochimwa zawo. 2 Petro 1:11, 20; 3:18
- **“Mbuye wa ulemelero”** kutanthauzo ubwino wa chilengedwe cha ulamuliro wake. 1 Akorinto 2:8
- **“Mbuye wa ambuye”** kutanthauza kuti ulamuliro wake umaposa ulamuliro wina uliwonse. Chivumbulutso 19:16
- **“Mbuye wa mtendere”** kusonyeza kufuna kwake kugwiritsa ntchito ulamuliro wake kuti abweretse mtendere pakati pa Mulungu ndi munthu. 2 Atesalonika 3:16
- **“Mbuye wa dzotuta”** kutanthauza ulamuliro wake pa kufalikira kwa uthenga wabwino. Mateyu 9:38; Luka 10:2
- **“Mbuye wa sabata”** kusonyeza ulamuliro wake pa lamulo la chinayi pa malamulo khumi. Mateyu 12:8; Luka 6:5
- **“Mbuye wolungama”** kusonyeza kuti iye ndi mulingo komanso opereka kulungama kwathu. Yeremiya 23:6; 33:16
- **“Mamuna wosonyezedwa kwa inu wochokera kumwamba”** zomwe zikutisonyeza kuvomerezedwa kwake ndi Mulungu. Machitidwe 2:22
- **“Mamuna wochokera kumwamba”** kusonyeza chilengedwe chake. 1 Akorinto 15:47
- **“Mamuna wazisoni”** kusonyeza chisoni chake kwa anthu amene amamukana. Yesaya 53:3

- **“Bwana”** kusonyeza ukulu wake pa ulamuliro kapena luso. Luka 5:5; 8:24, 45; 9:33; 17:13; Aefeso 6:9; Akolose 4:1; 2 Timoteo 2:21
- **“M’khalapakati wa pangano latsopano”** kutanthauza kuti iye ndi amene anaika chipangano cha tsopano ndi Mulungu. Ahebri 9:15; 12:24
- **“Wansembe wamkulu wachifundo ndi okhulupilika”** kutanthauza chisoni ndi kusasintha kwa udindo wake. Ahebri 2:17
- **“Mtumiki wa pangano”** amene azibweretsa nkhani za pangano latsopano ndi Mulungu. Malaki 3:1
- **“Mpulumutsi”** kutanthauza kuti anasankhidwa ndi Mulungu kuti apulumutse anthu ku machimo awo. Yohane 1:41; 4:25
- **“Mulungu wa mphamvu”** zomwe zikutanthauza mphamvu zake. Yesaya 9:6
- **“Nyenyezi yowala m’mawa”** kutanthauza kuti iye ndi nyenyezi yowalitsitsa kuposa zinzake zomwe zazungulidwa ndi m’dima. 2 Petro 1:19; Chivumbulutso 22:16
- **“M’nazareti”** lomwe ndi dzina la anthu onyozedwa. Mateyu 2:23
- **“Mwana wa Davide”** kutanthauza umoyo wa umunthu wake unadutsa mu mtundu wa mfumu Davide. Chivumbulutso 22:16
- **“M’modzi ndi Atate”** kutanthauza mgwirizano wa Mulungu. Yohane 10:30
- **“Mwana wakubadwa yekha wakukhala pa chifuwa cha Atate”** zomwe zikuonetsa umunthu wake. Yohane 1:14, 18
- **“Mulungu yekha mpulumutsi wathu”** kutanthauza umunthu wake ndi ntchito zake. Yuda 1:25
- **“Mbuye wathu ulemelero”** zomwe zikusonyeza ukulu wa ulamuliro wake kwa omukhulupilira. Yakobo 2:1
- **“Mulungu ndi mpulumutsi wathu”** zomwe zikusonyeza ubale wa umunthu wake ndi ntchito zake za ku mpingo. 2 Petro 1:1
- **“Moyo wathu”** kutanthauza chiyambi chimene anapereka ku mpingo. Akolose 3:4
- **“Mbuye wathu”** kusonyeza kuvomereza kwa mpingo ulamuliro wake. Aroma 1:4; 5:21; 7:25; 1 Akorinto11:9; Yuda 1:25
- **“Mfumu ndi mbuye wathu yekha”** kutanthauza kuvomereza kwa mpingo ukulu ndi ulamuliro wake. Yuda 1:4
- **“Chotupitsa chathu”** zomwe zikutanthauza nsembe yake m’malo mwa mpingo. 1 Akorinto 5:7
- **“Mtendere wathu”** zomwe zikutanthauza chiyambi cha mtendere pakati pa Mulungu ndi mpingo. Aefeso 2:14
- **“Mpulumutsi wathu”** kutanthauza kuchotsa kwa machimo kumene anapereka ku mpingo. Tito 3:6
- **“Sing’anga”** zomwe zikuonetsa kuthekera kwake kuchiritsa. Luka 4:23
- **“Mtsogoleri ndi mpulumutsi”** kutanthauza munthu amene amasogolera moyo ndi chipulumutso. Machitidwe 5:31
- **“Mtsogoleri wa moyo”** kutanthauza kuti amasogolera moyo. Machitidwe 3:15
- **“Mtsogoleri wa mtendere”** kusonyeza kuti amasogolera kuyambitsa mtendere ndi Mulungu. Yesaya 9:6
- **“Mtsogoleri wa atsogoleri”** kusonyeza kuti palibe msogoleri wina oposa iye. Danieli 8:25
- **“Mulosi”** zomwe zikuonetsa kukwaniritsa kwake kwa ulosi. Deutronomo 18:18 cf. Machitidwe 3:22
- **“Chiombolo cha machimo athu”** kusonyeza kuti anaonetsa kulungama ndi chilungamo cha Atate. 1 Yohane 2:2
- **“Woyeretsa”** zomwe zikutanthauza ntchito zake zochotsa machimo kwa anthu. Malaki 3:3
- **“Chinyezimiro cha ulemelero wake”** zomwe zikutanthauza kuwalitsa kwa chikhalidwe cha Atate. Ahebri 1:3
- **“Chiombolo cha onse”** kutanthauza kuti anadzipereka kuti tipulumuke. 1 Timoteo 2:6
- **“Kuuka ndi moyo”** zomwe zimatiphunzitsa kuti kuuka nkukhala ndi moyo wosatha zimapezeka kudzera kwa Yesu Khristu. Yohane 11:25
- **“Woweluza olungama”** kutanthauza kuti amasogolera khalidwe kapena amapereka mphatso kutengera ndi khalidwe lake labwino. Masalmo 7:11; 2 Timoteo 4:8
- **“Olungama”** zomwe zikuloza kuika umunthu wake wabwino pa chikhalidwe chake chabwino. Yesaya 24:16; Machitidwe 3:14; 7:52; 22:14; 1 Yohane 2:1

- **“Mnsinsi wa Davide”** kusonyeza kuti chilengedwe chake chosatha chinatenga nawo mbali pomupanga Davide. Chivumulutso 22:16
- **“Olamura ma ufumu a dziko lapansi”** zomwe zikutanthauzira ulamuliro wake oposa maulamuliro akuluakulu a padziko lapansi. Chivumbulutso 1:5
- **“Mpulumutsi wa dziko”** kusonyeza kuti ndi iye yekha angapulumutse ku machimo. Yohaane 4:42; 1 Yohane 4:14
- **“Mbusa”** kuonetsera chisamaliro chake kwa amene amawakonda. Genesis 49:24; Masalmo 80:1; Mlaliki 12:11
- **“M’busa wa mizimu yathu”** kuti onetsera chisamaliro chake kwa gawo la mkati mwa munthu. 1 Petro 2:25
- **“Chizindikiro cha anthu”** kutanthauza kuti iye ndi munthu amene anthu ayenera kumufuna. Yesaya 11:10
- **“Mwana wa Mulungu”** zomwe zikuonetsa ubale wake ndi utatu wa Mulungu. Yohane10:36; 11:14
- **“Mwana wa Mulungu wa moyo”** zomwe zikuonetsa ubale wake ndi Mulungu weniweni osati fano. Mateyu 16:16
- **“Mwana wa Mulungu wa m’wambamwamba”** zomwe zikutanthauza m’mene angelo amamuonera. Marko 5:7; Luka 8:28
- **“Chiyambi cha chipulumutso chosatha”** zomwe zikutanthauza kuti ndi chachipulumutso. Ahebri 5:9
- **“Kukhazikitsa kwa moyo wathu”** kutanthauza kuvutika kwake ali moyo. Yesaya 33:6
- **“Mwala”** kutanthauza kukhazikika kwake pa moyo wa munthu. Yesaya 28:16
- **“Mwala umene omanga nyumba anaukana”** kutanthauza kukhazikika kumene asogoleri a Israeli anasankha kusutsana nako. Masalmo 118:22; Mateyu 21:42; Marko 12:10; Luka 20:17; 1 Petro 12:7
- **“Mphunzitsi” (Rabboni)** kutanthauza kuthekera kwake kophunzitsa. Yohane 20:16
- **“Mwala woyetsedwa”** zomwe zikutanthauza zimene Yesu anakumana nazo pa moyo wake. Yesaya 28:16
- **“Umboni wobadwa nthawi yake”** kutanthauza umboni wa Yesu umene unaululidwa mogwirizana ndi Mulungu mu nthawi yabwino. 1 Timoteo 2:6
- **“Mkate woona”** kutanthauza kuti Yesu ndi chakudya chenicheni cha cha moyo wa uzimu kapena uMulungu. Yohane 6:32
- **“Kuwala kowona”** kutanthauza zenezeni za vumbulutso lake la choonadi. Yohane 1:9; 1 Yohane 2:8
- **“Mpesa woona”** kutanthauza kuti Yesu ndi opereka mzimu wa chipatso cha uzimu (ntchito zabwino). Yohane 15:1
- **“Choonadi”** kutanthauza ubwino wa gawo lililonse la moyo wake. Yohane 5:33; 8:31-32; 14:6
- **“Njira”** kutanthauza kuti iye ndi chiyambi cha chipulumutso komanso utsogoleri wabwino. Mateyu 7:14; Yohane 14:5-6
- **“Chuma chachipulumutso”** kutanthauza m’mene amaonera kufunika kopulumutsa munthu. Yesaya 33:6
- **“Nzeru”** kutandauza kuti ali ndi kuthekera komvetsetsa ndi kugwiritsa bwino ntchito chilichonse chopezeka mmau a Mulungu. Yesaya 33:6
- **“Amene anayesedwa kwa ife chilungamo ndi chiyeretso ndi chiomboro”** kutanthauza kuti chipulumutso ndikukula muuzimu zimapezeka mu umunthu wake osati chilichonse. 1 Akorinto 1:30
- **“Amene anakhala nzeru ya kwa Mulungu kwa ife”** kutanthauza kuti nzerunso amapereka kwa anthu ake. 1 Akorinto 1:30
- **“Mboni kwa anthu”** kutanthauza umboni umene amapereka kwa anthu onse. Yesaya 55:4
- **“Mlangizi wabwino”** kutanthauza kuthekera kwake kopereka chithandizo chabwino chomwe chimafunikira nthawi ya mavuto. Yesaya 9:6
- **“Mau”** kutanthauza kuti ndi chiyambi cha chiyankhulo chonse. Masalmo 119:81; Yohane 1:1,14; 1 Yohane 1:1; Chivumbulutso 19:13
- **“Mau a Mulungu”** kutandauza kuti amapezeka pakulumikizana kulikonse ndi Mulungu. 2 Petro 3:5: Yohane 1:1-5; Chibvumbulutso 19:13
- **“Mau a moyo”** kutanthauza kuti iye ndi chiyambi chomanga zonse za moyo. Afilipi 2:16; 1 Yohane 1:1
- **“Mamunawako”** kutanthauza kuthekera kwa ubale wa anthu ndi iye. Yesaya 54:5
- **“Ondilenga ine”** kutanthauza kuti iye ndi mlengi wa anthu onse. Yesaya 54:5

- **“Mpulumutsi wako”** kutanthauza kuti iye ndi amene analipira machimo onse a anthu. Yesaya 54:5
- **“Chipulumutso chako”** kutanthauza kuti iye ndi amene amachotsa zochimwa za anthu. Luka 2:29-30

Zoyenera kuchita aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Mutu 5, Gawo 4

1. **Werengani Akolose 1:16 ndi Yohane 8:58. Kodi tikumva chiyani za umunthu wa Yesu Khristu?**

2. **Werengani Mateyu 22:41-46. Kodi Mesiya anakhala bwanji Ambuye komanso mwana wa Davide?**

3. **Werengani 1 Petro 2:22. Kodi izi zitanthauza chiyani za uchimo mu moyo wa Khristu?**

4. **Werengani Yesaya 7:14, 9:6, 11:1-2, 53:2. Lembani nkhani yaifupi pa za Mesiya yemwe adzabwera?**

5. **Werengani ndime izi ndipo fotokozani zomwe imfa ya Yesu inapanga kwa ife?**
   a. Agalatiya 3:1
   b. Akolose 1:13-14
   c. Aefenso 2:14-16
   d. 1 Yohane 2:1-2

6. **Werengani nkhani izi ndipo fotokozerani za kuuka kwa Yesu kwa akufa?**
   a. Mateyu 27:62-66
   b. Yohane 20:2-10
   c. Yohane 20:14, Mateyu 28:9-10, Yohane 20:26-29, 21:1-23, 1 Akorinto 15:6
   d. 1 Akorinto 15:1-3

7. **Werengani Machitidwe 1:9 ndi Akolose 3:1. Khristu anachitanji atauka kwa akufa?**

8. **Werengani nkhanizi ndipo fotokozani zomwe Yesu akuchita pamene wakhala kudzanja lamanja la Atate?**
   a. Ahebri 7:25
   b. 1 Yohane 2:1
   c. 1 Timoteo 2:5
   d. Ahebri 4:14

9. **Werengani Aefenso 1:22-23. Kodi Yesu ndi ndani ku Mpingo?**

10. **Werengani Yohane 10:11, Ahebri 13:20 ndi 1 Petro 5:4. Kodi ‘Ambuye’ ndi M’busa wanji?**

11. **Pezani malongosoledwe a umunthu wa Mwana mu gawo ‘D’ Mokhudzana ndi ntchito zake zomwe ziri m’musimu (1, 2, 3).**
    a. Kupezeka kwake dziko lisanakhalepo
    b. Kulumikizana kwake ndi Mulubgu
    c. Chiyero chake
    d. Kubadwa kwake ndi moyo wake
    e. Imfa yake
    f. Kuukanso kwake kwakufa
    g. Kukwera kwake kumwamba komanso kukhala kwake pa dzanja la manja la Atate
    h. Utumiki wake

Gawo 5
Mulungu Mzimu (Chiphunzitso cha Mzimu Woyera-Pneumatology)

A. Umunthu Wake[100]

Umboni unaperekedwa kale kuti Mzimu Woyera ndi Mulungu. Mzimu Woyera ndi munthu, osangoti dzina logwiritsidwa ntchito kuonetsa mphamvu zake. Izi zinaperekedwera umboni wake potengera kuti iyeyu ali ndi zikhalidwe zitatu zonse za munthu: kuganiza (Nzeru), kukhuzidwa ndi kusankha (chifuniro).

Pakhala kusagwirizana kwambiri kutengera mu mbiri ya mpingo mu phunziro la umunthu ndi ntchito za Mzimu Woyera. Tiyenera kuyang'ana mosamala pa lamuro loti ***"ndikusamalitsa kusunga umodzi wa Mzimu mwa chimangiriro cha mtendere"*** (Aefeso 4:3). Kumvetsetsa kowona ndi kudalira Mzimu Woyera zingatisogolere ku chikondi (Agalatiya 5:22) chimene sichimangokhala chikondi chathu kwa Mulungu komanso kwa wina ndi nzake (1 Yohane 4:20).

Kachisi wa Mzimu Woyera ndi thupi la Khristu. Mtumwi Paulo anafunsa, ***"mumadziwa kuti*** (kutanthauza nonse) ***thupi*** (limodzi) ***ndi kachisi*** (kutanthauza thupi limodzi komanso kachisi mmodzi) ***wa Mzimu Woyera amene ali mwa inu, amene muli naye kuchokera kwa Mulungu komanso kuti simuli anu nokha?"*** (1 Akorinto 6:19). Mbuyomo ku 1 Akorinto Paulo anafunsa fuso lofanana, ***"mumadziwa kuti*** (nonse) ***ndinu*** (ambiri) ***kachisi*** (chimodzi) ***wa Mulungu, ndiponso kuti mzimu wa Mulungu amakhala mwa*** (nonse) ***inu?"*** (1 Akorinto 3:16). Mzimu Woyera amalumikiza anthu mu thupi la Khristu kwa wina ndi nzake. Tinachenjezedwa kuti tisaononge kachisiyo. Ndi m'chitidwe osayera (1 Akorinto 3:17). Pali mkwati m'modzi yekha wa Yesu Khristu. Izi zikhale chotsogoleria pa phunziro ili:

1. **Nzeru**
   Mzimu Woyera ali ndi kuthekera kodziwa ndi kufufuza zinthu za Mulungu (1 Akorinto 2:10-11). Izi zimatiphunzitsa kuti ali ndi maganizo (Aroma 8:27) komanso kuthekera kophunzitsa anthu (1 Akorinto 2:13).

2. **Kukhuzidwa**
   Mau aMulungu amanena kuti Mzimu Woyera akhoza kumvetsedwa chisoni (Yesaya 63:10; Aefeso 4:30) zomwe zikuonetsa kuti amakhuzidwa. Akanakhala kuti iye ndi mphamvu chabe, sibwenzi akumakhunzidwa ndi zinthu monga mmene mphamvu ngati yamagetsi siingakhunzidwe ndi china chilichonse. Izi zili chomwechi chifukwa choti akhoza kuchitilidwa mwano (Marko 3:29). Umachitira mwano munthu osati mphamvu.

3. **Kusankha**
   Ndizodziwikanso kuti ali ndi kuthekera kosankha. Mzimu Woyera mu ufumu wake amagawa mphatso za uzimu ku thupi la Khristu (1 Akorinto 12:11). Ndizodziwikanso kuti amathandidzira ndi kutsogolera zintchito za akhristu (Machitidwe 16:6-11).

4. **Maonekedwe**
   Kamodzi kokha mmalemba, pobatizidwa Yesu Khristu, ndipamene tinaona Mzimu Woyera kutenga maonekedwe a nkhunda kusonyeza mtendere (Mateyu 3:16; Marko 1:10; Luka 3:22; Yohane 1:32).

Zoyenera kuchita aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Mutu 5, Gawo 5A

1. **Tchulani zinthu zitztu zimene zimasonyeza umunthu?**
   a. Werengani 1 Akorinto 2:10-11. Kodi tikuphunzirapo chiyani za Mzimu Woyera?
   b. Werengani Aefenso 4:30. Kodi tikuphunzirapo chiyani za Mzimu Woyera?
   c. Werengani 1 Akorinto 12:11. Kodi tikuphunzirapo chiyani za Mzimu Woyera?

B. Ntchito Zake

1. **Kulenga**
   Ndizachiziwikire kuti Mzimu Woyera anatenga mbali polenga ndi kukonza kumwamba ndi dziko lapansi. Pamene dziko linali losatheketsetsa komanso lopanda anthu ***"Mzimu wa Mulungu unali ukuyenda pa mwamba pa madzi"*** (Genesis 1:2) ngati mbalame imafungatila chisa chake kutetezera ana ache (Deutronomo 32:11). Malemba amati ambuye analenga kumwamba pomangoyankhura "mau" ndiponso mkuti Mzimu Woyera unaika nyenyezi (Masalmo 33:6). Mzimu Woyera alinso ndi mphamvu pa chilengedwe chake (Yobu 26:13).

Mzimu Woyerayo alinso ndi ntchito pa chilengedwe ndi kukonzedwa kwa munthu (Yobu 33:4) komanso kukonza kwa zinyama (Masalmo 104:24-25 cf.104:30).

Ntchito yake pa chilengedwe ndi kuvumbulutsa mbuye Mulungu kudzera muchilengedwe chake (Yesaya 40:12-13 cf. Aroma1:20 cf. Yohane 16:13-14).

2. Vumbulutso

Ntchito ya Mzimu Woyera mu vumbulutso ndikudziwitsa anthu chilungamo chatsopano (Yohane 16:13). Umagwiritsa ntchito a tumiki a anthu kuti anene chilungamo (2 Samueli 23:2) ndipo nthawi zina chilungamocho chimakhala nkhani yoipa (Mika 3:8).

Malembanso pawokha ndi chivumbulutso chochokera kwa Mzimu Woyera (Mateyu 22:42-43; Machitidwe 1:16; 4:24-25; 28:25-26; Ahebri 10:15-16).

3. Kumvetsetsa

Mzimu Woyera amavumbulutsa uthenga wa uzimu kwa anthu, koma wina ndiwovuta kuwumvesetsa (1 Akorinto 13:12). Ndiyeno Mzimu Woyera amathandiza kuti timvetsetse mau a Mulungu (1 Akorinto 2:12-16) ndiponso ma gawo a mau a Mulungu amene tingagwiritsa ntchito mu njira zosiyanasiyana zomwe timakumana nazo pa moyo (Luka 12:11-12; Ahebri 3:7-8). Kugwiritsa ntchito kumvetsetsa kwa uzimu ku moyo kumatchulidwa kuti "nzeru."

4. Kuganiza Bwino

Mzimu Woyera unapangitsa anthu ena kuti alembe malemba woyera (2 Petro 1:21). Timauzidwa ndi mawu a Mulungu kuti "malemba onse ndi m'pweya wa Mulungu" kutanthauza kuti "ali ndi mzimu wa Mulungu" (2 Timoteo 3:16-17). Mtumiki Paulo pamene amalemba mauwo anagwiritsa ntchito mau a chi Greek amene samapezeka pena paliponse. Ndi mau oti THEOPNEUSTOS omwe ndi mau amene anapangidwa ndi mau a chi Greek THEOS komanso PNEUMA kutanthauza kuti "Mulungu" komanso "mzimu." Buku lonse loyera linapangidwa ndi Mulungu Mzimu Woyera.

5. Zozizwitsa

Yesu amachita zozizwitsa ndi mphamvu ya Mzimu Woyera (Luka 4:18).

Mzimu Woyera analinso okhuzidwa ndi zozizwitsa zina ndi zina. Chitsanzo chimodzi chodziwika ndi pamene Filipo anabatidza munthu wa ku Ethiopia kenako ndikusowa (Machitidwe 8:39). Chinanso ndi kubadwa kwa Yesu mwa namwaliyo.

6. Kubadwa mwa namwaliyo

Maliya, namwaliyo anauzidwa ndi ngelo Gabrieli kuti azabereka Mwana amene adzapatsidwe ndi Mzimu Woyera ndipo adzatchulidwa "Mwana wa Mulungu" (Luka 1:27, 35). Gawo ili sili kungotiuza kuti ndi uti mu utatu mwa Mulungu wa kumwamba amene anali tate wa Yesu, komanso ndi umboni wina otiuza kuti Mzimu Woyera ndi Mulungu.

Pamene Maliya anakhara ndi pakati pa Yesu Khristu, ngelo anaonekera kwa Yosefe, mamuna amene anali pa ubwenzi ndi Maliya kuti akwatirane, ndipo anamuuza kuti Maliya anali ndi pakati pa Mzimu Woyera (Mateyu 1:18-20).

7. Kutsutsa za Tchimo

Ntchito ina ya Mzimu Woyera ndi kutsutsa anthu za tchimo. Izi zikutanthauza kuti amakonza osati dziko lokha komanso anthu amene sanasatire malamulo a Mulungu, potero kuti ndiwochimwa, ndipo akusowekera mpulumutsi (Yohane 16:8). Amawapeza anthu olakwa kuchokera ku tchimo mu chikumbumtima chathu (Aroma 9:1).

8. Kukonzanso

Kukonzanso ndi mau amene amatanthauza kubadwanso mwa tsopano. Ndikulongosora zomwe zimachitika pa chipulumutso osati chipulumutso chitatha. Mzimu Woyera ndi amene amapereka kubadwa mwatsopano kutsatira lonjezo la Mulungu mu mau ake (1 Petro 1:23 cf. Tito 3:5).

9. Ubatizo

Kwakhala chisokonezo kwambiri kwa a Khristu pokhuza ubatizo wa Mzimu Woyera. Tiyeni tione bwinobwino zimene bukhu loyera limakamba pa phunziro ili.

Mau amu chi Greek a "ubatizo" (BAPTIZO) amatanthauza "kuviika" ndipo amagwiritsidwa ntchito ndi ma Greek kufuna kuonetsa "kuviika kwa chovala" kapena kutunga madzi poviika chotungira kuchina

kapena kuposedwa ndi mafunso.[101] Pamene ubatizo kapena kuviika (Monga munthu m'madzi, kapena mkondo kuviika magazi nkhondo isanayambe) Kunali chizindikiro kapena kuzipeleka kwa munthu wina kapena choyambitsa. Inali njira yoonetsa mgwirizanowo kaya polemba, kuthupi kapena maganizo, linapangidwa ndi gulu lina kapena zochitika. Mwachitsanzo Yesu anati ali ndi "ubatizo" womwe akumane nawo zomwe zimaimilira mtanda (Marko 10:38) chifukwa ubatizo wake wamadzi unali utachitika kale (Marko 1:9). Ubatizo wamadzi wa Yesu Khristu kunali kuvomereza dongosolo la Mulungu pa moyo wake.

Uthenga wa Yohane m'batizi unaika lonjezo lonena kuti mpulumutsi ***"adzabatiza ndi Mzimu Woyera"*** (Mateyu 3:11; Marko 1:8; Luka 3:16; Yohane 1:33; Machitidwe 1:5). Ndiyeno ubatizo wa Mzimu Woyera sunachitike kufikira pamene ambuye anatumiza Mzimu Woyera pa tsiku la Pentekoste (Yohane 14:16-17; Machitidwe 2:1-4) umene Petro anautchura kuti "chiyambi" (Machitidwe 11:16). Sichinali chinthu chimene okhulupilira analandira ingakhale mmbuyomu kupatula pa tsikulo. Chinali chatsopano kwa mpingo pamene zinayamba pa tsiku la Pentekoste.

Ndizovuta kumvetsa ubatizo wa Mzimu Woyera popanda kudziwa kuti cholinga chake chinali kuika okhulupilira pa tsiku la Pentekoste "muthupi" lodziwika kuti "thupi la Khristu" (1 Akorinto 12:12-13) kapena mpingo (Aefeso 5:22-30). Dziwani kuti tchimo silimachotsa munthu aliyense ku "thupi" chifukwa zikanakhala choncho akorinto akanachotsedwano werengani (1 Akorinto 1–11 chifukwa amachita machimo osiyanasiyana).

Palibe lamulo lililonse m'mau a Mulungu lonena kuti "batizidwani ndi Mzimu Woyera" choncho ndi china chake chomwe chimachitika pamene munthu wakhulupilira Yesu Khristu, kuvomereza ifa yake, kuikidwa ndi kuuka kwake (1 Akorinto 15:1-4). Si ubatizo wonyowa koma wouma.

Choonadi cha ubatizo wa uzimu kwa okhulupilira zinalembedwa bwinobwino ndi Paulo mtumiki. Iye anati:

> ***Kapena kuti simudziwa kuti ife tonse amene tinabatidzidwa tinabatidzidwa mwa Khristu Yesu; tinabatizidwa mu imfa yake? Chifukwa chake tinailkidwa m'manda pamodzi ndi iye mwa ubatizo kulowa mu imfa; kuti monga Khristu anaukitsidwa kwa akufa mwa ulemelero wa Atate kotero kuti nafenso tikayenda m'moyo watsopano. Pakuti ngati tinakhala olumikizidwa ndi iye mchi faniziro cha imfa yake, kotero tidzakhala mchifanizidwe cha imfa yake, koteronso tizakhala mchifanizidwe cha kuuka kwake*** (Aroma 6:3-5).

Ubatizo wa Mzimu Woyera umene okhulupilira amakhala atazazidwa ndi mzimu woyera (Yohane 14:17; Aroma 5:5) ndiyeno, umachitika pamene munthu wavomereza Yesu Khristu ngati mpulumutsi wake ndipo amadziwika ndi zintchito zake pa iwo.

10. Chizindikiro kapena chidindo (chisindikozo)

Chidindo chikutanthauza maonekwe atsopano kapena osinthika amene amapangidwa monga chitsulo ukachimata. Ayuda anapanga izi pamanda a Yesu Khristu, kuti azadziwe ngati mwala otseka pa manda a Yesu Khristu wachotsedwa (Mateyu 27:66). Mzimu Woyera amaika chitseko chosaonekera cha Mulungu kwa munthu amene akukhulupilira Yesu Khristu (Aefeso 1:13).

Ndi choikika kutu munthu amene ali ndi chidindo chimenechi wavomerezedwa. Wokhulupilirayo walowa mu mgwirizano osatha ndi Yesu Khristu ndipo Mzimu Woyera "amadinda dzina lake" mu mgwirizano umenewo. Mzimu Woyera monga Mulungu amagwiritsa ntchito chidindo cha Mulungu (2 Akorinto 1:22) kuti apange chizindikilo chosaoneka ndi maso.

Chifukwa choti Mzimu Woyera anawagwirizanitsa okhulupilira tiyenera "tisamumvetse chisoni" pochita uchimo (Aefeso 4:30).

Kwanenedwa kuti "tatsindikizidwa kufikira tsiku la chipulumutso" (Aefeso 1:13-14; 4:30) zomwe zikutanthauza tsiku lamtsogolo limene chipulumutso chathu chidzamalizidwa pa kuuka (Aroma 8:23).

11. Kulowa ndi kukhala kwa Mzimu Woyera mwa okhulupilira

Kulowa ndi kukhala kwa Mzimu Woyera mwa okhulupilira kunachitika pa nthawi ya chipulumutso. Izi zinali choncho pofuna kukwaniritsa lonjezo lomwe Yesu anapanga lomwe anati, ***"ndipo ine ndidzapempha Atate, ndipo adzakupatasani inu nkhoswe ina, kuti akhale ndinu ku nthawi zonse, ndiye mzimu wachoonadi, amene dziko lapansi silingathe kumlandira iye, chifukwa silimuona iye, kapena kumuzindikira iye. Inu mumzindikira iye; chifukwa akhala ndinu, nazakhala mwa inu"*** (Yohane 14:16-17).

Litsanafike tsiku la Pentekoste, zinanenedwa kuti Mzimu Woyera "unakhala" pa okhulupilira. Kuyambira tsiku la Pentekoste, kunanenedwa kuti ali "m'kati" kapena "kukhalira" mkati mwa okhulupilira. Mokhala mwa Mzimu Woyera ndiyeno mufanana ndi mu mpingo (Aroma 8:9; 1 Akorinto 3:16; 6:19; 2 Timoteo 1:14).

Mautumiki akuluakulu a Mzimu Woyera monga kutsutsa tchimo ndi kuvumbulutsa choonadi, sanasinthe ndo omwewo koma anasintha pokhala.

Kulowa kwa Mzimu Woyera mkati mwa okhulupilira kumachitika nthawi imodzi ndi ubatizo wa Mzimu Woyera, pa nthawi ya chipulumutso. Chifukwa choti ubatizo komanso kulowa kwa Mzimu Woyera ndi mphatso zochokera kwa Mulungu (Machitidwe 11:16-17; Aroma 5:5), sizingachotsedwe (Aroma 11:29). Kulowa kwa Mzimu Woyera sikumahotsedwa ndi tchimo lochitidwa ndi okhulupilira monga timawonera ku mpingo wa Akorinto. Pa 1 Akorinto 1:2; 3:16 komanso 6:19, okhulupilira ku Korinth ananenedwa kuti ndi opulumutsidwa kusatengera machimo ambiri amene Paulo anawafotokoza ku mutu 5 ndi 6.

Pali zochitika ziwiri zimene zinalembedwa mu buku la Machitidwe pamene Mzimu Woyera unaperekedwa chitatha chipulumutso (Machitidwe 10:44; 19:1-6). Ndichiyembekezo chathu kuti ophunzira akukumbukira kufunsa mafunso monga "ndani?" "chani?" komanso "nthawi zanji?" Nthawi zambiri anthu amene amakhuzidwa amakhulupilira kuti mpulumutsi adzabwera koma samadziwa kuti wabwera kale. Atauzidwa kuti mpulumutsi wabwera ndipo atakhulupilira uthengawo, kenakono analandira Mzimu Woyera. Sichinthu cha nzeru kudikilira zochitika zopatulika kenakono nkukhulupilirano kuti zimachitika.

12. Kudzazidwa

Mu phunziro lathu laku dzazidwa ndi Mzimu Woyera, tipitanso ku mau a Mulungu kuti tipeze mayankho. Tiona kalongosoledwe ka kudzazidwa ndi Mzimu Woyera mu buku loyera kenako tiona kufunika kwake pa moyo wathu.

a. Kudzazidwa ndi Mzimu Woyera ndi:

1) Koperekedwa pochita ntchito zosiyanasiyana monga zaluso komanso usogoleri

Kudzazidwa ndi Mzimu Woyera kunaperekedwa mu nthawi ya Israeli kwa anthu osiyanasiyana kuti achite ntchito zosiyanasiyana. Mzimu Woyera amatha kufunsidwa (Luka 11:13), koma sizinali zoyenera. Malemba analemba kuti zinaperekedwa kwa Bezelali, m'modzi mwa ogwira ntchitoyo kuti luso lake likhale lotamanda Mulungu (Eksodo 31:3; 35:31). Imanenanso kuti ***"Yoswa anadzazidwa ndi mzimu wa nzeru"*** (Deutronomo 34:9) kuti asogolere Israeli atamwalira Mose.

2) Koperekedwa kwa utumiki wa paderadera, chilimbikitso ndi ulosi

Muuthenga wabwino wa Luka tinapeza kuti Yohane m'batizi (Luka 1:15) mayi ake Elizabeti (Luka 1:41) ndi bamboo ake Zekaliya (Luka 1:67) anadzazidwa ndi Mzimu Woyera. Zitsanzozi zimaonetsa kuti "kudzazidwa ndi Mzimu Woyera ndi umboni wa mphamvu yake umene unaperekedwa kuti uchite ntchito yapaderadera.

3) Koperekedwa pa chiyankhulo cha paderadera kwa anthu osiyanasiyana

Yesu atauka koma asanakwere kumwamba, anaudza ophunzira ake kuti "alandire Mzimu Woyera" (Yohane 20:22), uwu ndi umboni woti amvere Mzimu Woyera (Machitidwe 1:2) ndiponso kuti adikire kudzoza kwake (kupereka kwa mphamvu) zomwe zizachitike m'masiku obwerawo (Machitidwe 1:8). Izi ziwapatsa chisomo choti akhululukire amene anapachika Yesu Khristu (Yohane 20:23).

Pamene Mzimu Woyera unawapatsa mphamvu powadzaza pa tsiku la Pentekoste, anayamba kuyankhura ziyankhuro za amitundu zomwe sanadziweko (Machitidwe 2:1-11 makamaka ma: esi 4, 8, 11). Petro anapatsidwa mphamvu yakulalikira zomwe zinalembedwa mavesi omwewo (2:14-40) ndiponso kupereka lonjezo la Mzimu Woyera kwa onse amene anavomereza uthenga wa Yesu Khristu (2:38-40). Ndi umboni wakuti nthawi ya Israeli, kudzoza kwa Mzimu Woyera kumafuna mphamvu yapaderadera kuti munthu achite ntchitoyo.

4) Koperekedwa ku kuzikanira ku uzimu komanso kulimbika mtima

Zinthu zina za kudzaza kwa Mzimu Woyera zinachitika pamene Petro ananenaa chozikanira kwa ayuda (Machitidwe 4:5-12) kenako nkupereka uthenga wa chozikanira kwa anzake. Petulo ndi anzakewo anadzazidwa ndi Mzimu Woyera ndipo anali ndi mphamvu yakuyankhula mau molimbika mtima (Machitidwe 4:31).

Mudziwe kuti mphamvu ziwirizi sizinakhuze kuyankhula ziyankhulo za mitundu. Ndiyeno chikhulupiliro chakuti kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera kumakhuza kuyankhura malilime nthawi zonse ndi bodza.

Kutengera zitsanzo zimene zaperekedwa kale za kudzoza kwa Mzimu Woyera, tikhoza kudziwa kuti Mzimu Woyera amalowa ndi kukhala mwa okhulupilira kamodzi ndipo zimakahala zokhazikika. Kudzazidwa ndi Mzimu Woyera kumachitika kwambiri komanso sikokhazikika. Umboni wina wa mfundoyi ndi wakuti okhulupilira samalamulidwa kuti kuti Mzimu Woyera "akhale mwa iwo" koma amalamulilidwa kuti "adzazidwe" (Aefeso 5:18). Mokhala mwa Mzimu Woyera mumakhuza malo (Mzimu Woyera mwa ife ndipo ife mwa Khristu). Pamene kudzoza kwa mzimu kwa Mzimu Woyera kumakhuza kuonetsa mphamvu yake kudzera mwa okhulupilira.

5) Koperekedwa kuti apereke mphamvu utumiki wake
Kudzaza kwa Mzimu Woyera kunaikidwa mu mpingo kuti kupereke mphamvu ku zintchito zathu za utumiki kwa okhulupilira ena. Pamene vuto limapezeka mu mpingo wakale zokhuza chisamaliro pa akazi amasiye (Machitidwe 6:1), ophunzira khumi ndi awiri anaudza mpingo onse kuti asankhe amuna akhalidwe amene anadzazidwa ndi mzimu komanso nzeru kuti akonze vutoli (Machitidwe 6:2-5), ndipo mpingowo unachita zomwezo. Ophunzirawo anaona kufunika kwa mphamvu ya Mzimu Woyera kwa anthu kuti azitumikira mu mpingowo.

6) Koperekedwa kuti adziwe chinyengo cha Satana
Sauli (Paulo), paulendo wake oyamba otumikira Mulungu, amapereka mau a Mulungu kwa kazembe wa chi Roma dzina lake Sergio paula ndipo anasutsidwa ndi wa masenga dzina lake Elima (Machitidwe 13:6-7). Paulo modzazidwa ndi Mzimu Woyera anadziwa kuti Elima amafuna kuipisa mau a Mulumgu (Machitidwe 13:8-10).

7) Koperekedwa kuti athane ndikukanidwa
Umboni wina wakudzazidwa ndi Mzimu Woyera ukuwonekanso pamene Paulo ndi Barnaba anakanidwa ndi a yuda ku sunagoge ya pisidiya (Machitidwe 13:42-51). Kudzaza kwa Mzimu Woyera mugawoli kukusonyeza kuti ubale wawo ndi Mzimu Woyera ukupitilirabe pa utumiki wawo (13:52).

b. Kudzazidwa ndi Mzimu Woyera kwa Khristu amene akukula
Chifukwa choti okhulupilira analamulidwa kudzazidwa ndi Mzimu Woyera (Aefeso 5:18), tikhoza kunena motsindika kuti siokhulupilira aliyense amene amakhala odzazidwa nthawi zonse.

Chifukwa choti tchimo limasokoneza ubalewa okhulupilira ndi Mulungu, chomwechonso limalepheletsa kuti akhale odzazidwa ndi Mzimu woyera (1 Yohane 1:6).

Okhulupilira amayenera kumayenda moyo wodzazidwa ndi Mzimu Woyera tsiku ndi tsiku, ndipo umoyo umenewu umatchulidwa kuti "Kuyenda mu kuunika" (Yohane 8:12; 12:35-36; Aefeso 5:7-10; 1 Yohane 1:7). Nthawi zina okhulupilira amachimwa (1 Yohane 1:8, 10). Tchimo limeneli limaononga ubale wathu ndi Mulungu, ndipo okhulupilirayo ayenera kulapa machismo ake, kuvomereza ndi chikhulupiliro kuti Mulungu ndi "okhulupilika ndi wolungama, kuti atikhululukire machismo athu,ndi kutisambitsa kutichotsera chosalungama chilichonse" (1 Yohane 1:9).

Chonde tidziwe kuti kudzaza kwa Mzimu Woyera kwakhala mchitidwe omalizika, chochitika nthawi yomweyo (pompopompo) ndipo osati mchitidwe osamalizika. Palibe chitsanzo cha munthu amene anadzazidwa kapena osamalizidwa kudzozedwa ndi Mzimu Woyera, ndipo kudzazidwa kwa Mzimu Woyera sikumatenga kukula kwa munthu mu uzimu. Ndiyeno kudzaza kwa kwa Mzimu Woyera: (1) ndikopezekera kwa okhulupilira onse, osatengera kukula kwawo komanso (2) ndikomalizika. Tiyeneranso tidziwe bwinobwino kuti chifukwa chakuti Mzimu Woyera akhoza kukanidwa (Machitidwe 7:51) munthu ayenera kudzipeleka yekha kwa Iye kuti adzazidwe.

Kuchokera ku mfundo tapezazi, tikhoza kunena kuti kudzoza kwa Mzimu Woyera ndi ntchito yaphumphu yogwirika yomwe imapereka mphamvu okhulupilira kuti azikhala moya wa chi Khristu. Komabe, chochitikachi si cholinga cha moyo wa Chikhristu koma ndi gawo lofunukira kwambiri limene limayambitsa ndi kusunga moyo wa Chikhristu.

Zinthu zinai zosonyeza kukhala wodzazidwa ndi Mzimu Woyera ndi izi: kuthekera kotamanda Mulungu (zooneka kunja), kulambira Mulungu (zimachitika mkati mwa moyo), kuthokoza Mulungu komanso kudzipereka kwa wina ndi nzake (Aefeso 5:19 -21).

13. Kupemphera

Mugawo la kudzaza kwa Mzimu Woyera tinaona ubwino wa kukhazikika. Tinaphunzitsinsanso kuti ndi kwabwino "kupemphera mu uzimu" kusonnyeza ubale wathu ndi Mulungu Mzimu Woyera (Aefeso 6:18; Yuda 1:20-21). Mu moyo wathu wa pemphero, ndizofunika kuti tizikhala muchiyanjano ndi Mulungu pamene tikupemphera, ndekuti tiyenera kukhazikika nkulapa machimo athu (1 Yohane 1:9).

Pazakhala nthawi imene sitizatha kupemphera, sitimadziwa mau oti tigwiritse ntchito kapenano zimene tikufuna kunena. Pamene izi zachitika, tikhoza kukhala ndi chilimbikitso chifukwa Mzimu Woyera amatipembedzera ife kuti mapemphero athu afike kwa Atate (Aroma 8:26-27).

14. Kutsimikizira

Gawo lina la ntchito ya Mzimu Woyera ndi kumutsimikizira okhulupira za chipilumutso komanso madalitso osatha. Tinauzidwa kuti ***"amachitira umboni… kuti ndife ana a Mulungu"*** komanso kuti ndife ***"olowa amzache a Khristu"*** (Aroma 8:16-17).

Mzimu Woyera ndi "lonjezo" la cholowo chathu chosatha (Aefeso 1:13-14).

15. Kupembezera

Mzimu Woyera amaonesetsa kuti Atate adziwe zofuna zathu ngakhale pamene sitinathe kudzitchura (Aroma 8:26-27).

16. Kupeleka mphatso

Yesu Khristu pamene anankwera kupita kwa Atate, anapereka mphatso kwa anthu (Aefeso 4:11). Mphatso za uzimuzi zimagawidwa kwa okhulupilira ndi Mzimu Woyera (1 Akorinto 12:11, 18; Ahebri 2:4).

Mphatso ya uzimu ndi kuthekera koperekedwa ndi Mulungu kwa okhulupilira kuti akapambane (kudutsa kuthekera kwa munthu) magawo ena apaderadera pa moyo kuti akapindulire thupi la Yesu Khristu (1 Akorinto 12). Okhulupilira wina laiyense ali ndi mphatso ndipo ayenera kuzigwiritsa ntchito kuti akatumikilire okhulupilira ena (1 Petro 4:10).

Ingakhale kuti mphatso ya Mzimu Woyera siyachilengedwe kapena yotengera (kuphunzira), Mzimu Woyera amagwiritsa ntchito luso la chilengedwe lathu komanso kuthekera kudzera mu mphatso ya uzimu. Luso la maimbidwe mwachitsanzo likhoza kuonetsedwa kedzera mu mphatso ya kuphunzitsa kapena kulangiza (Aroma 12:8).

Muyeneranso kukhala ndi kuthekera kwachibadwidwe kapena kophunzira kuti mphatso yanu ya uzimu igwire bwino ntchito. Mwachitsanzo ngati unapatsidwa mphatso ya chiphuzitso (Aroma 12:7; 1 Akorinto 12:28; Aefeso 4:11) uyenera kuwerenga mau a Mulungu (2 Timoteo 2:15) ndikuphunzira m'mene ungawaphunzisire.

Tipitiliza chiphuzitso cha mphatso za mzimu oyera mu Mutu 8)

17. Chiphunziso

Ntchito yofunikira ya Mzimu Woyera ndikutiphunzitsa ife zinthu za Mulungu (Yohane 14:26). Akhoza kutiphunzitsa ife mwachangu potengera ndi kufunikira kwake (Luka 12:11-12) kapena akhoza kutisogolera ife mu gawo lophunzira (Yohane 16:13-15).

Ndikuzera mu utumiki wophunzitsa wa Mzimu Woyera yekha basi mmene ife timaphunziradi zinthu za uzimu (1 Akorinto 2:10-16).

18. Kutsogolera

Mzimu Woyera ndi msogoleri wathu mu umoyo wathu wa chikhriitu. Monga msogoleri wathu, ntchito yake yeniyeni ndikutiphunzitsa ife za Yesu Khristu (Yohane 16:13) kuti tikhale ngati iye (1 Akorinto 11:1; Aefeso 5:1).

Pamene chifunilo cha Mulungu chawonekera bwinobwino bwino bwino kupyolera mmau ake, monga pokhuzana ndi chikhalidwe (1 Timoteyo 1:8-11: Aroma 8:12:14), chisogoza za Mzimu Woyera chimakhala chodziwikiratu. Popeza kuti Mzimu Woyera anawauzira mawu a Mulungu (2 Timoteyo 3:16-17; 2 Petro 1:21), tikhonza kudziwa chifunilo chake kuchokera pa zimene zinalembedwa ndipo ndizimene zimatisongolera ife.

Pamene chofunilo cha Mulungu chavumbulusidwa bwinobwino kudzera m'mau ake, monga kufuna kusankha pakati pa zinthu ziwiri zabwino, tiyenera tidzipereke tokha kwa iye "ngati nsembe ya moyo ndi yoyera" (Aroma 12:1) kuti tizindikire zofuna zake (Aroma 12:2).

Zitsanzo zina za utsogoleri wa Mzimu Woyera, werengani Machitidwe atumwi 8:29; 10:19-20; 13:2-4; 16:6-7; 20:20-23.

19. Kubala Zipatso
Mzimu Woyera amene amakhalira mwa ife amakhumbira kubala zipatso kudzera mwa ife. Chiipatso chake ndi "chikondi, chimwemwe, mtendere, kuleza mtima, chifundo, kukoma mtima, chifatso, chikhulupiliro, chiletso" (Agalatiya 5:22-23). Kuti izi zichitike, tiyenera timulore Mzimu Woyera kuti apereke mphamvu ku umoyo wathu wa Chikhristu (Agalatiya 5:16, 25) kuti thupi lathu ndi zintchito zake za uchimo zigonjetsedwe (Agalatiya 5:17-21).

20. Kubweretsa Chimwemwe ndi Chisangalalo
Mzimu Woyera amabweretsa chimwemwe mwa ife komanso chisangalalo chimene chimachoka mwa ife. Chimwemwe chimenechi chikhoza kubwera ingakhale pa nthawi ya masautso (1 Atesalonika 1:6). Chimwemwe ndi chisangalalochi zimabwera powona m'dalitso wa Atate kwa anthu ena ndipo osangoti mdalitso wako wekha basi (Luka 10:21).

21. Kutsanulira Chikondi
Pamene Mzimu Woyera walowa mwa amene amakhulupilira Yesu Khristu, amabweretsa chikondi chowona cha Mulungu komanso chiyembekezo chimene sichingakhumudwitse (Aroma 5:5).

22. Kuvumbulutsa chilungamo, Mtendere ndi Chimwemwe
Mumoyo wa okhulupilira, Mzimu Woyera amavumbulutsa kuti m'dalitso ofunikira kwambiri wa mu ufumu wa Mulungu ndi wa uzimu osati wa kuthupi (Aroma 14:17).

23. Kupereka Mphamvu
Mzimu Woyera amabweretsa mphamvu kwa okhulupilira kuti okhulupilirayo akhale ndi chiyembekezo chosaneneka (Aroma 15:13) komanso kuti okhulupilira alalikire uthenga wabwino wamuyaya komanso wakumwamba (1 Petro 1:12).

24. Kuyeretsa
Tinayeretsedwa kwa Mulungu kuti tizitha kupereka kwa Mulungu nsembe zovomerezeka zamatamando komanso kuchita zabwino kwa ena (Aroma 15:16 cf. Ahebri 13:15-16). Kuyeretsedwaku kumakhuza chikhalidwe chathu chifukwa amene amachita khalidwe loipa amachedwesedwa ndipo sapita chitsogolo pa moyo wawo wa uzimu (1 Atesalonika 4:1-8). Gawo la kuyeretsedwa kwathu ndikulora mzimu "woyera" kuti "atiyeretse" monganso iye ali "woyera" (1 Petro 1:16).

25. Kukhazikitsa chiyanjano
Mzimu Woyera ndi amene amakhazikitsa ubale kapena chiyanjano pakati pa anthu okhulupilira, kutengera chisomo cha Yesu Khristu komanso chikondi cha Atate (2 Akorinto 13:14).

Zoyenera kuchita aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Mutu 5, Gawo 5B

2. Werengani ma vesi awa ndipo longosolani ntchito za Mzimu Woyera

a. Yobu 33:4
b. Yohane 16:13
c. 1 Akorinto 2:12-16
d. 2 Petro 1:21
e. Luka 4:18
f. Luka 1:27 ndi 35
g. Yohane 16:8
h. Tito 3:5
i. Mateyu 3:11
j. Aefenso 1:13
k. Yohane 14:16-17
l. Aefenso 5:18
m. Aefenso 6:18
n. Aroma 8:16-17
o. Aroma 8:26
p. 1 Akorinto 12:11 ndi 18
q. Yohane 14:26
r. Agalatiya 5:22-23
s. 1 Atesalonika 1:6
t. Aroma 5:5
u. Aroma 14:17
v. Aroma 15:13
w. Aroma 15:16
x. 2 Akorinto 13:1

C. Kulongosola za Mzimu Woyera

- **"Nthandizi wina"** Kutathauza utumiki wake otonthoza ndi kulimbikitsa ngati wa Yesu. Yohane 14:16
- **"Mpweya wa Mulungu wa mphamvu zonse"** kutanthauza mphamvu zake kupereka moyo. Yobu 32:8; 33:4

- **"Mphatso"** kutandauza kupezeka kwake pokhala mphatso yochokera kwa Mulungu. Machitidwe 2:38; 8:19-20; 10:45
- **"Nthandizi"** kutanthauza chilimbikitso chake powaphunzitsa anthu chilungamo. Yohane 14:16
- **"Chikole"** kutanthauza chizindikiro chopatsidwa kwa ife chokhuza chipulumutso chathu. 2 Akorinto 1:22; 55:5; Aefeso 1:14
- **"Olonjezedwa"** kutanthauza ntchito yake mu dongosolo la Mulungu. Machitidwe 2:33; Aefeso 1:13
- **"Mzimu wolera"** kutanthauza ntchito yake yotitengera ife mu banja la Mulungu. Aroma 8:15
- **"Mzimu wa chiweruzo ndi otentha"** kutanthauza kulungama kwake ndi choonadi chake ngati Mulungu. Yesaya 4:4
- **"Mzimu wa Khristu"** kutanthauza ntchito yake mu umunthu wa Yesu Khristu. Aroma 8:9; Afilipi 1:19; 1 Petro 1:11
- **"Mzimu wa uphungu ndi mphamvu"** kutanthauza kukhuzidwa ndi chithandizo chimene amapereka kwa iwo akusowa. Yesaya 11:2
- **"Mmzimu wa chikhulupiliro"** kutanthauza kuyenera kwake kuti tizimukhulupilira. 2 Akorinto 4:13
- **"Mzimu wa ulemelero"** kutanthauza ufumu wake. 1 Petro 4:14
- **"Mzimu wa Mulungu"** kutathauza chikhalidwe chake cha Mulungu. Genesis 1:2; Eksodo 31:3; 35:31; Numeri 24:2; 1 Samueli 10:10; 11:6; 19:20, 23; 2 Mbiri 15:1; 24:20; Yobu 33:4; Masalmo 106:33; Ezekieli 11:24; Mateyu 3:16; 12:28; Aroma 8:9, 14; 1 Akorinto 2:11, 14; 7:40; 12:3; Aefeso 4:30; Afilipi 3:3; 1 Yohane 4:2
- **"Mzimu wakumwamba"** kutanthauza chikhalidwe chake monga Mulungu. Genesis 41:38
- **"Mzimu wa chisomo ndi wakupembedza"** kutanthauza kupeleka kwake kwa chisomo ndi kumvetsera mapemphero. Zekariya 12:10
- **"Mzimu wa Mwanawake"** kusonyeza kuimilira utatuwo woyera. Agalatiya 4:6
- **"Mzimu wa kuyera"** kutanthauza kuti iye si Mzimu Woyera yekha chabe komanso kuti amaulura za kapena kuwonetsera chiyero. Aroma 1:4
- **"Mzimu wa chiweruzo"** kutanthauza vumbuluso lake la chiweruzo. Yesaya 4:4
- **"Mzimu wa chilungamo"** zomwe zikuimira kusakondera kwake. Yesaya 28:6
- **"Mzimu wachidziwitso ndi owopa ambuye"** kutanthauza chiziwiso chimene iye amapereka chimene chimasogolera kulemekeza ambuye. Yesaya 11:2
- **"Mzimu wamoyo"** kutanthauza ntchito yake yopereka moyo wa uzimu. Aroma 8:2
- **"Mzimu wa Mulungu wathu"** kutanthauza ntchito yake yakuwonetsera Mulungu mu mpingo. 1 Akorinto 6:11
- **"Mzimu wa Mulungu wa moyo"** zomwe zili kusiyanitsa Mulungu ndi mafano. 2 Akorinto 3:3
- **"Mzimu wa ambuye"** kutanthauza chithandizo chake kwa mfumuyo. Luka 4:18; Machitidwe 5:9; 8:39; 2 Akorinto 3:17
- **"Mzimu wa Mulungu ambuye"** kutanthauza chithandizo chake kwa Mulungu amene ndi mfumu. Yesaya 61:1
- **"Mzimu wa chilungamo"** chifukwa palibe bodza mwa iye. Yohane 14:17; 15:26; 16:13; 1 Yohane 4:6
- **"Mzimu wa nzeru ndi wakumvetsa"** kutanthauza kuthekera kwake komvetsetsa komanso kugwiritsa bwino ntchito mau aMulungu m'moyo. Yesaya 11:2
- **"Mzimu wa nzeru ndi chivumbulutso"** kutanthauza kuthekera kwake kosogolera munthu mu kagwiritsidwe nchito ka mau a Mulungu kuti Khristu aziwike kwambiri. Aefeso 1:17
- **"Mau a wamphamvu"** kutanthauza ntchito yake ngati woyankhura mau a Mulungu. Ezekieli 1:24
- **"Mau a mbuye"** zomwe zikutanthauza za kuyankhura kwake kwa ulamuliro wa ukulu. Yesaya 6:8

Zoyenera kuchita aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Mutu 5, Gawo 5C

3. **Tengani malongosoledwe a Umunthua Mzimu Woyera mu 'C' Ndipo fanizirani ndi ntchito zake m'mausimu. Perekani yankho limodzi a. b.**
   a. Ntchito yake
   b. Umunthu wake

Chaputala 6

Magawo a Zopanga Mulungu

Gawo 1
Chilengedwe (Cosmology)

Vesi loyamba mu buku loyera limatiuza kuti ***"pachiyambi Mulungu analenga kumwamba ndi dziko lapansi."*** Genesis 1:1. Mau a mu chi hebri amene amatanthauzira "chilengedwe" ndi mau oti BARA amene amatanthauza kuti "kuyambitsa chinthu chatsopano"[102]
osaiwalanso mfundo yakuti "kulenga chinthu posachokera ku chinthu china."[103] Mulungu yekha amanene amene amabweletsa zinthu za tsopano kapena kupangitsa kuti zinthu zatsopano zikhalepo.

Zokuti Mulungu analenga kumwamba ndi dziko lapansi zinalembedwa m'mavesi angapo m'mu buku loyera (Yesaya 40:26-28; 42:5; 45:12, 18). Ndizofunika kuti tivomereze mfundo imeneyi pakuti imayankha limodzi mwa mafunso akulu kwa anthu lakuti "Munthu anachokera kuti? Yankho ndi lakuti Mulungu analenga munthu.

Olemba buku la Ahebri anatiuza kuti, ***"ndi chikhulupiliri tizindikira kuti maiko ndi a m'mwamba omwe anakonzedwa ndi mau a Mulungu,kotero kuti zinthu zopenyeka sizinangidwa zochokera mwa zoonekazo"*** (Ahebri 11:3). Izi zimatiphunitsa kuti Mulungu analankhura ndikubwerera kumwamba kuti kukhalepo. Chilengedwe chinakhalapo ndi ulamuliro komanso mphamvu za Mulungu, osati chifukwa chakusintha kwa zinthu ndi nyengo (Masalmo 33:6; 148:4-5).

Baibulo limanenanso kuti Mulungu analenga moyo wonse (Genesis 1:21) kuphatikizapo moyo wa munthu (Genesis 1:27; 5:2; 6:7; Yesaya 45:12) kenako "anapuma" ku chilengedwe chake (Genesis 2:3-4). Sikulina msogolo, azalenga kumwamba kwa tsopano ndi dziko lapansi la tsopano (Yesaya 65:17; 2 Petro 3:10-13; Chivumbuluso 21:1).

Zoyenera kuchita aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Mutu 6, Gawo 1

1. **Werengani Genesis 1:1. Kodi analenga kumwamba ndi dziko lapansi ndi ndani?**
2. **Werengani Ahebri 11:3. Kodi Mulungu anawalenga iwo motani?**
3. **Werengani Genesis 1:2-31. Kodi Mulungu analenganso chiyani china?**
4. **Werengani 2 Petro 3:10-13, Chibvumbulutso 21:1. Kodi Mulungu adzalenga chiyani mtsogolo?**

Gawo 2
Angelo (Angelology)

A. Umunthu Wawo

Mawu a Mulungu amatiuza kuti pali chilengedwe cha anthu anzeru oposa anthufe otchedwa Angelo. Angelowa anatchulidwa malo ochuruka mu Baibulo Kuchoka ku Genesis kufika ku Chibvumbulutso. Tanthauzo lenileni la 'ANGELO' Mu chi Hebri, komanso mu chi Greek ANGELOS' Ndiko kuti Mnthenga kapena 'otumidwa.' Angelowa amatha kuganiza komanso kulankhula. Popeza iwo ali ndi nzeru (Mateyu 8:29; 2 Akorinto 11:3; 1 Petro 1:12), amamva kuwawa (Luka 2:13; Yakobo 2:19; Chibvumbulutso 12:17) komanso ali ndi mpata wosankha (Luka 8:28-31; 2 Timoteyo 2:26; Yuda 6). Angelowa ndi anthunso ndithu.

Angelo ndi mizimu (Ahebri 1:14) komabe angathe kutenga chifanizo cha munthu, movemerezedwa ndi Mulungu (Luka 2:9; Luka 24:4). Angelo ndi anthu amphamvu,omwe ali paudindo wapamwamba oposa munthu (Ahebri 2:7). Izi zikusonyeza kuti iwo ali ndi mphamvu komanso nzeru zochuruka koposa munthu (Chibvumbulutso 10:1-3). Koma angelo samadziwa zinthu zonse (1 Petro 1:12) kapena kukhala ndi mphamvu zonse (Mateyu 25:41) ngati Mulungu, ndiponso angelo samapezeka ponseponse.

Tapatsidwa maina atatu okha a angelo mu Mawu a Mulungu. Ndipo pali (1) Mikayeli (Danieli 10:13, 21; 12:1; Yuda 1:9; Chibvumbulutso 12:7), (2) Gabrieli (Danieli 8:16; 9:21; Luka 1:19, 26), (3) Satana (Chibvumbulutso 12:9).

B. Yemwe Anawalenga

Angelo analengedwa ndi Mulungu (Masalimo 148:2-5) pa nthawi ina yakale, Mulunguyo asanapange dziko lapansi (Yobu 38:7). Podziwa kuti angelo sabereka ana, monga munthu achitira (Luka 20:35) ndipo angelo samafa (Luka 20:36), chiwerengero cha angalo chiri chimodzimodzi. Ngakhale timamva kuti angelo ndi ochuruka koma sitikudziwa kuti chiwerengero chawo ndi chotani (Ahebri 12:22; Chibvumbulutso 5:11).

Timadziwa, komanso timavomereza kuti Mulungu ndi woyera (Mateyu 5:48) komanso opanda tchimo (2 Akorinto 5:21). Podziwa kuti Mulungu ndi wangwiro, kukhalanso kosavuta kunena kuti amalenga zinthu za moyo muungwiro, wopanda tchimo, popeza "Alibe Choipa mwa Iye" (Masalimo 5:4). Izi zikukambanso kuti Satana analengedwa ndi Mulungu opanda tchimo, koma kumapeto kwake iye anasankha kusutsana ndi Mulungu (Ekekieli 28:12-15; Yesaya 14:12-14).

Anthu ena amakhulupilira kuti angelo ndi anthu amoyo omwe anafa kale ndikudzuka. Apa tiyenera kusutsa, chifukwa angelo analengedwa anthu asanapangidwe. Angelo ndi Olengedwa Opatulidwa.

C. Dongosolo Lawo

Timadziwa kuti angelo ali ndi maudindo osiyanasiyana, chifukwa iwo ali kuonetseredwa ngati ali pa Msonkhano (Masalimo 89:5, 7), ndipo ali okonzekera nkhondo (Chibvumbulutso 12:7).

Mngelo wa udindo wamuulu kwambiri ndi 'Mgelo Wankulu.' potengera dzina lakelo lotanthauza ngelelo wolamulira angelo anzake. Mikayere (Yuda 9). Yemwe amatchedwa "kalonga wamkulu" (Danieli 10:13), Iyeyu amatsogolera angelo a Mulungu pa nkhondo yolimbana ndi Satana (Chibvumbulutso 12:7). Choncho, pali Mgelo Wamkulu M'Modzi. Iyeyu ali nawo mawu apaderadera (1 Atesalonika 4:16).

Tikuonanso kuti angelo angathe kugwira ntchito ngati "olamulira" (Aroma 8:38; Aefenso 1:21; 3:10; 6:12; Akolose 1:16; 2:10, 15), "udindo" (Aefenso 1:21; 2:2; 3:10; 6:12; Akolose 1:16; 2:10, 15; 1 Petro 3:22), "mphamvu" (2 Petro 2:11), "apampando" (Aefenso 1:21; Akolose 1:16; 2 Petro 2:10; Yuda 1:8). Awa ndi maumboni a maudindo ndi ntchito zawo za angelo mudziko la angelo.

Pali magulu ena awiri a angelo otchedwa "Aserafi" ndi "Akerubi." Aserafi atchulidwa mu chaputala chimodzi chokha mu Baibulo, ndipo akulongosoledwa kuti ali ndi mapiko asanu ndi limodzi. Komanso ali ndi thupi longa la munthu (Yesaya 6:2, 6). Aserafi ndi angelo omwe amayeretsa pogwiritsa ntchito moto. Dzina loti Serafi limatanthauza 'kupsereza.'

Akerubi Ndi gulu linanso la angelo omwe ali ndi maudindo chifukwa Satana anali m'modzi wa iwo (Ezkieli 28:14, 16). Munthu atachimwa (Adamu ndi Hava), ndikuchotsedwa munda wa Edeni, Akerubi anagwiritsidwa ntchito yolondera kuti anthuwa asapitenso ku mtengo wa moyo mu Edeni (Genesis 3:24).
Tikupeza kuti Akerubi anaimikiridwa mu Likasa la Yehova monga gawo limodzi la pangano (Eksodo 25:18-22), Chinsalu (Eksodo 26:1), Chophimba (Eksodo 26:31). Mose anamva Ambuye akulankhula kwa iye kuchokera ku Mpando wachifundo ndi Akerubi awiri (Numeri 7:89).

Akerubi ndi gawo lofunikira kwambiri la kachisi wa Solomo. Pali awiri a iwo omwe anapangidwa kuchokera ku mtengo wa Azitona, osakanizidwa ndi Golidi, omwe utali wawo unali Mamita 5, okhala ndi mapiko aatali mapazi khumi ndi asanu (15 feet) (1 Mafumu 6:23-28). Mapiko awo aphimbira pa Likasa la Pangano (1 Mafumu 6:29-35). Ndipo iwo amaikidwa pa zipangizo za m, kachisi (1 Mafumu 7:29, 36).

M'Masomphenya, kwa mneneri Ezkieli, tikupeza Akerubi akuyesedwa Chipinda cha ufumu cha Mulungu (Ezkieli 10:1-22). Pali chimvemvemve kuchokera mu nusu wa malembo amene amatchula iwo kuti Akerubi ali ndi nkhani zofunika mu mbiri, ngakhale kuti ena amaona zovuta kumvetsa. Ntchito yawo siinathe ayi popeza idzafunikanso pa kachisi wa zaka chikwi (Ezkieli 41:18, 20, 25) yemwe udzabwera mtsogolo.

Zomveka ndi chodziwika bwino chokhudzana ndi Akerubi ndi zoti iwowa ndi ofunika komanso aphindu pa dongosolo la Mulungu. Mu maphunziro ena,mtsogolomu, tiona ntchito yawo mwatsatanetsatane.

D. Utumiki Wawo

Angelo akhala akupezeka komanso kugwira ntchito pa mbiri ya munthu. Iwo anakhala nawo pa kupembedzera ndi kukondwerera pamene Ambuye anapanga dziko lokhalamo (Yobu 38:6-7). Iwowa anagwira nawo ntchito pa kupereka malamulo khumi kwa Mose (Agalatiya 3:19; Ahebri 2:2) komanso kawirikawiri anagwira ntchito pa bvumbulutso la choonadi cha Mulungu (Danieli 7:15-27; 8:13-26; 9:20-27; Chibvumbulutso 1:1; 22:6, 8). Angelo amakhuzidwa osati ndi Israeli yekha (Danieli 12:1), komanso mafuko ena (Danieli 4:17; 10:21; 11:1; Chibvumbulutso 8:9, 16).

Angelo ananeratu za kubadwa kwa Yesu (Mateyu 1:20) anachenjeza makolo a Yesu kuti athawire ku Aegupto (Mateyu 2:13-15) nawauza nthawi yochokera ku Aegupto (Mateyu 2:19-21), anatumikirapo kwa Yesu atangoyesedwa kumene ndi Satana (Mateyu 4:11) komanso mmene anali munda wa Getsemane (Luka 22:43). Anapezekanso pa kuuka kwa Yesu (Mateyu 28:1-2), komanso pomwe Yesu ankakwera kupita kumwamba kwa Atate (Marko 1:10-11).

Angelo amagwira ntchito nthawi imene mpingo utangoyamba kumene powauza alaliki kuti apite kwa anthu omwe akonzekera kumva uthenga wabwino (Machitidwe 8:26; 10:3) kupereka masomphenya kwa osowa upangiri (Machitidwe 10:3, 7) kubweretsa mayankho ku pemphero komanso kuwapulumutsa anthu ku zoopsa (Machitidwe 12:11). Angelo adzakhalanso okangalika pa zochitika mu nthawi ya kubweranso kwa Yesu Khristu (Mateyu 25:31; 2 Atesalonika 1:7), kuphatikizapo pa chiweruzo (Chibvumbulutso 7:1; 8:2).

Angelo amatamanda Mulungu (Masalimo 148:1-2; Yesaya 6:3) kupembeza Iye (Ahebri 1:6; Chibvumbulutso 5:8-13) ndi kuchita chifuniro cha Mulungu (Masalimo 103:20; Chibvumbulutso 22:9).

Angelo anagwiranso ntchito pa kupereka chiweruzo kwa anthu osalungamai. Angelo amalalikira za chiweruzo chili nkuza (Genesis 19:13; Chibvumbulutso 14:6-7; 19:17-18), amapelekanso chilango mwa chiweluzo molamulidwa ndi Mulungu (Machitidwe 12:23; Chibvumbulutso 16:1) ndipo adzagwiritsidwa ntchito yolekanitsa olungama ndi osalungama (Mateyu 13:39-40).

Angelo akupitilirabe kuthandiza okhulupilira (Ahebri 1:14), ndipo timamvanso kuti "Tisasiye kuchereza alendo, poteropo ena anachereza angelo, ngakhale samadziwa" (Ahebri 13:2). Amachita chidwi nkumaona zomwe akhristu amachita (1 Akorinto 4:9) ndipo amaphunzira kuchokera kwa ife (Aefenso 3:8-10; 1 Petro 1:10-12) mu nyengo zina iwo amabwera ndikuzatilimbikitsa mu nthawi ya kusowa (Machitidwe 27:23-24), tikafa, angelo adzatitenga ife kupita nafe kwathu kumwamba (Luka 16:22).

E. Satana

1. Satana Ndi Ndani?

Satana ndi chinthu chonga munthu yemwe ali ndi nzeru (2 Akorinto 11:3) amamva (Chibvumbulutso 12:17; Luka 22:31) ndi kuthekera kosankha (Yesaya 14:12-14; 2 Timoteo 2:26). Pali anthu ena omwe amakhulupilira kuti Satana sali cholengedwa koma kuti ndi mphamvu ya choipa basi. Yesu Khristu ananenetsa kuti Satana adzalandira chilango chopita mu nyanja yamoto (Mateyu 25:41). Mungathe kuona kuti mphamvu ya choipa singalangidwe, choncho kusakhulupilira kuti Satana ndi wolengedwa monga munthu ndi kukayikira kapena kusakhulupilira pa choonadi cha Yesu Khristu. Satana wakhala akugwilitsa ntchito njira zobweretsa chikaiko pa mawu a Mulungu kuyambira mu munda wa Edeni (Genesis 3:1-5).

2. Chinachitika ndi Chiyani?

Satana anali Kerubi wa udindo wapamwamba yemwe analengedwa wolungama ndi wopanda uchimo koma kenako anachimwa (Ezkieli 28:12-15 komwe 'Mfumu yak u Turo,' ikugwiritsidwa ntchito monga chitsanzo kutiphunzitsa ife za zomwe zinachitika kwa Satana. Mfumu yaku Turo inali ndi munda wokongola, koma sunali munda wa Edeni). Miyala ya Mtengo wapatali yomwe inali chophimba chake

(28:13) komanso pokhala kuti kuti anadetsa kachisi kapena malo opatulika" (28:18), zikusonyeza kuti iye anali Mkulu wa Nsembe wa angelo. Monga Mkulu wansembe komanso mu kuchuruka kwa ntchito zake (kuzikweza yekha udindo), Iye anakopa ndi kusocheletsa gawo limodzi la magawo atatu a angelo (Chibvumbulutso 12:4).

Satana anaganiza zolimbana ndi Mulungu. Izi zikupezeka mu Yesaya 14:12-14. Uchimo wake unali kuzikuza (1 Timoteyo 3:6) monga umapezekera mu mmalankhulidwe ake ozikweza oterewa: (ndichita zimene ndikufuna osati zimene Mulungu akufuna) monga zinalembedwera ku Yesaya. Satana ndi yemwe analenga tchimo (Ezkieli 28:15) ndipo adzayankha mulandu wolenga tchimolo (Mateyu 25:41) chifukwa zinachokera mu mtima mwake (Yesaya 14:13).

Kuzikweza kwake koyamba Satana anati "Ndidzakwera kumwamba" kusonyeza cholinga chake chofuna kufanana ndi Mulungu. Kachiwiri anati "Ndidzakweza mpando wanga wa chifumu pa mwamba pa nyenyezi za Mulungu," Kutanthauza kuti Satana khumbo lake ndi kulamulira chilengedwe cha angelo kumwamba. Pozikudza kachitatu ananena kuti "Ndidzakhala pa phiri, kumpoto." Apa zimasonyeza Milungu ya Babulo, komanso Babulo analamulira dziko lonse lapansi. Khumbo lake lachinayi "Ndidzakwera pamwamba pa mitambo" kusonyeza kuti iye akufuna ulemelero wa Mulungu" (yemwe amakhudzana ndi mitambo). Khumbo lachisanu "Ndidzakhala monga wamwambamwamba" kusonyeza khumbo lake la ulamuliro ndi mphamvu yofuna kutenga malo a Mulungu.

Titatha kuphunzira za Tchimo la Satana, kuli kophweka kuti tione chifukwa chomwe ife timalangizidwa "kusachita chinthu kuchokera mu kukuzikuza/kuzinyenga, koma ndi kuzichepetsa kwa malingaliro lolani aliyense wa inu awonane wina ndi mzake monga wofunikira koposa iye mwini" (Afilipi 2:3). Ngati tiri ndi kuzikuza, maganizo atokha, tikufanana ndi Satana.

3. Maina ndi Maudindo a Satana

Maina ndi maudindo omwe Satana anapatsidwa ndipo amagwiritsa ntchito akutionetsera poyera za makhalidwe ake. Iye amatchedwa 'Nyenyezi'/Nthanda wa Mbanda kucha (Yesaya 14:12). Kusonyeza 'Wonyamula Muuni' ndipo zimatanthauziridwa kuchokera ke mawu a chilatini "Lucifar." Yesu Khristu ndiye "Nyenyezi ya Mbandakucha" Yeniyeni (Chibvumbulutso 22:16). Zomwe zimatiphunzitsa kuti Satana ndi wabodza ponyengeza anthu kuti iye ndi Khristu, kuyambira nthawi ya kugwa kwake.

Iye amatchedwa SATANA. Dzinali linachokera ku chihebri "SATAN" kusonyeza kuti 'Wotsutsa' (Numeri 22:22, 32; 1 Samueli 29:4; 2 Samueli 19:22; 1 Mafumu 5:4; 11:14, 23, 25; 1 Mbiri 21:1; Jobu 1:6, 7, 8, 9, 12; 2:1, 2, 3, 4, 6, 7; Masalimo 109:6; Zakaliya 3:1, 2; Mateyu 4:10; 12:26; 16:23; Marko 1:13; 3:23, 36; 4:15; 8:33; Luka 10:18; 11:18; 13:16; 22:3, 31; Yohane 13:27; Acts 5:3; 26:18; Aroma 16:20; 1 MAchitidwe a Tumwi 5:5; 7:5; 2 Akorinto 2:11; 11:14; 12:7; 1 Atesalonika 2:18; 2 Atesalonika 2:9; 1 Timoteo 1:20; 5:15; Chibvumbulutso 2:9, 13, 24; 3:9; 12:9; 20:2, 7). Satana amazuza a Khristu nthawi zones (Chibvumbulutso 12:10), koma ambuye Yesu Khristu amatiteteza ife (1 Yohane 2:1-2). Satana amawakankhizira anthu ku uchimo (Genesis 3:1-5; Mateyu 4:3; 1 Atesalonika 3:5; Acts 5:3; 1 Akolinto 7:5).

Iye amatchedwa Dyerekezi. Dzinali lochokera ku mau achi Greek "DIABOLOS" kutanthauza "Wonyenga" (munthu amene amanena bodza la mzake). (Mateyu 4:1, 5, 8, 11; 13:39; 25:41; Luka 4:2, 3, 6, 13; 8:12; Yohane 6:70; 8:44; 13:2; Machitidwe 10:38; 13:10; Aefeso 4:27; 6:11; 1 Timoteo 3:6, 7; 2 Timoteo 2:26; Ahebri 2:14; Jakobo 4:7; 1 Petulo 5:8; 1 Yohane 3:8, 10; Juda 1:9; Chibvumbulutso 2:10; 12:9, 12; 20:2, 10).

Iye a matchedwa Njoka yokalamba, kumasulira kuchenjera ndi bodza lake (Genesis 3:1, 2, 4, 13, 14; 2 Akolinto 11:3; Chibvumbulutso 12:9, 14, 15; 20:2).

Satana amatchedwa "Chinjoka chofiira chachikulu" kutanthauza khalidwe lake lowononga ku nkhondo (Chibvumbulutso 12:3, 4, 7, 9, 13, 16, 17; 13:2, 4, 11; 16:13; 20:2).

Amatchedwa Belezebule kutanthauza[104] "Ambuye wa khamu la ziwanda dzinali linapatsidwa ndi a Yuda potchulira mwini wa ziwanda (Mateyu 10:25; 12:24, 27; Marko 3:22; Luka 11:15, 18, 19).

Mtumwi Paulo adamutchanso "Beliyali" kutanthauza kusayera ndi kuipa kwake (2 Akorinto 6:15).

Satana amatchedwa "wolamulira a dziko la pansi (Yohane 12:31), mulungu wa dziko lapansi (2 Akorinto 4:4), mkulu wa mphamvu za mlengalenga (Aefeso 2:2) ndi "wa mzimu wa kuchita tsopano mwa ana akusamvera" (Aefeso 2:2). Chomwe mau onsewa akunena ndi chakuti, Satana ndi m'dani weniweni wa Mulungu.

4. **Ntchito zake Tsopano**

Ntchito ya Satana yokhazikika ndiyo kulimbana ndi njira za Mulungu ndi cholinga choononga kuti akapambane ku zikhumbo zake zonenedwazo (Yesaya 14:12-14). Cholinga cha Satana ndi kufanizira njira za Mulungu ndi zake ndi cholinga chakuti anthu asamufunenso Mulungu. Adzagwiritsa ntchito njira ina iliyonse pofuna kupambana kuphatikizilapo angelo ake otchedwa "ziwanda" (1 Timoteo 4:1) ndi anthu " amene amazizembayitsa ngati atumiki a chilungamo" (2 Akorinto 11:13-15).

Malingaliro a Satana pakulimbana ndi Njira za Mulungu ndi ofuna kufikira malamulo onse a Mulungu kuti akaoneke ngati mwini wake pamene kuli kutsutsana ndi Mulungu. Chikhazikitso cha malamulo chichokera ku mau a chi Greek a dziko lapansi wotchedwa "COSMOS." Tanthauzo la likulu la mau "COSMOS" ndi lamulo. [105]

Pofuna kukwaniritsa malingaliro ake choyambirira Satana "amaphimba malingaliro" (2 Akorinto 4:4) ncholinga chakuti osakhulupilira asakavomereze uthenga wa Yesu Khristu ndipo amayesetsanso kulanda mau a choonadi amene amva kuchokera kwa Ambuye (Luke 8:12). Pophimba malingaliro a osakhulupilira, nthawi zambiri amagwiritsa ntchito chifaniziro cha chikhiristu chimene "chimangokhala nawo maonekedwe a chipembedzo koma mphamvu yake adaikana" (2 Timoteo 3:5). Maonekedwe ake ngati mkhristu pamene mkati mwake ndi satana (Mateyu 23:25-26). Njira yofananiza zikhulupiliroyi imatenga magawo ambiri kuphatikiza iliyonse yodzikaniza wekha (Akolose 2:16 -23) ku chizolowezi ndi kutsimikiza tchimo (Aroma 1:32; Chibvumbulutso 2:24). Satana adzagwiritsa ntchito chirichonse padziko la pansi pano kuti alepheletse aliyense kulowa mu ufumu wa Mulungu (Akolose 1:13; 1 Yohane 2:15-17).

Pamene munthu walandira Yesu Khristu kukhala mpulumutsi amagonjetsa dziko la pansi, njira imene satana wakhazikitsa (1 Yohane 5:4-5). Satana sadzawasiya apulumutsidwa anadza ngati "mbala" ku "dzaba, kupha ndi kuononga" (1 Yohane 10:10) chifukwa cha chidani chake kwa mitundu yonse (Masalimo 69: 1-4; Mateyu 10:22).

Chinthu chachikulu chimene iye amafuna ndi kuononga mboni zenizeni za Khristu kuti anthu ena asafune kulowa mu ufumu wa Mulungu. Amayesa okhulupilira ndikuwapangitsa kuti akhale ofanizidwa ndi makhalidwe kapena malamulo a dziko la pansi ndi zochita zake (1 Atesalonika 3:5; 1 Yohane 2:15-17). Amayesanso okhulupilirira kuwabisira kudzikonda kwawo (Machitidwe 5:1-3) ndipo amawayesa iwo kuwachimwitsa ku machitidwe oipa a dziko la pansi (1 Akorinto 7:5).

Satana "monga Mkango wobuma, afunafuna wina akamlikwire" (1 Petro 5:8). Zikutanthauza kuti amakhala akufunafuna kupeza wina agwetsedwe ku mayesero ake kuti akathe "kuneneza abale" (Chibvumbulutso 12:10). Adzayikanso zosangalatsa ndi zokomedwetsa zonse pa okhulupilira monga amalolezedwa ndi cholinga chakuti munthu abwelere mmbuyo ndikusiya kukhala ophunzira wa Ambuye Yesu (Luka 22:31).

Okhulupilira ayenera kumudziwa bwino Satana kamba ka chikhalidwe chake (Yohane 8:44) samatsata chilungamo. Adzagwiritsa ncthito aliyense komanso chirichonse pokwaniritsa cholinga chake.

F. Angelo a Satana

Angelo a Satana ndi okhawo omwe anasankha kuyenda naye, ndipo angelo ochuruka anamutsata (Chibvumbulutso 12:4) Angelowa amatchedwa 'Ziwanda'. Kapena kuti 'Mizimu yoipa' kuphatikizirapo zolengedwa zomwe zinaukira Mulungu pamodzi ndi Satana monga mfumu yawo (Mateyu 12:24). Mawu a chigiriki 'Ziwanda' akusonyeza 'kuti timilungu ta dziko lapansi.' Mizimu yoipa ikusonyeza mizimu yomwe imatsogolera munthu ku choipa. Monga tanena kale, Satana ali ndi adindo wosiyana mu ufumu wakewo. Ziwanda ndi zamphamvu (Maro 5:3; Machitidwe 19:16). Ndipo kudzera mu mphamvu yake, amagonjetsa anthu.

Angelo a Satana ali ndi nzeru zomwe zimaonekera pomuzindikira Yesu (Marko 1:24), kuzidzindikira za chilango chawo (Mateyu 8:29) Komanso amafuna kutukula chiphunzitso chawo cha bodza (1 Timoteo 4:1-3). Angelo a Satana amadziwa pulani ya chipulumutso cha Yesu koma amaikana (Yakobo 2:19).

Ntchito za angelo a Satana ndizo, kutsutsana ndi Mulungu. Iwo amafuna kusokoneza chifuniro cha Mulungu. Ziwanda zimagwiritsidwa ntchito pakupembeza mafano ndi za matsenga (Machitidwe 16:16). Kupembeza mafano kumachitika pamene munthu aika chinthu china patsogolo, nachipembeza monga Mulungu. Fano limapangidwa kuchokera ku mwala, kapena mtengo, kapena munthu (Chibvumbulutso 13:15). Munthu amatha kulambiranso nzeru zake za iye mwini (Yohane 5:39-40). Ziwanda zimakhumba kukakamiza munthu kuti azizilambira osati Mulungu.

Ziwanda zimalimbikitsa chipembezo chabodza. Chipembezo chonyenga ndi chikhulupiliro chomwe chimalimbikitsa za 'Mpulumutsi wopanda phindu' (Satana) (1 Yohane 4:1-4), Chipulumutso mu ntchito (1 Timoteo 4:3-4 cf. Aefenso 2:8-9), Kapena ufulu wochita ntchito za uchimo, poziyerekeza kuti ndi zabwino (Chibvumbulutso 2:20-24; Agalatiya 5:13; Aroma 6:1).

Ziwanda ziri ndi mphamvu zobweretsa matenda (Mateyu 9:33) kapena kusokoneza mutu (Marko 5:4-5) pa anthu. Komabe SIMATENDA ONSE omwe amabwera chifukwa cha ziwanda, ndipo Baibulo limalekanitsa matenda a ziwanda ndi matenda achilengedwe (Mateyu 4:24; Marko 1:32, 34; Luka 7:21; 9:1).

Ziwanda ziri ndikuthekera komulowa munthu (Luka 8:28-31), nyama (Luka 8:32-33). 'Kugwira anthu' kukutanthauza kukhala ndi mphamvu mkati mwa munthu. Popeza tamva kale kuti "Wamkulu ndi yemwe ali mwa inu, Mzimu Woyera," koposa yemwe ali m'dziko lapansi (1 Yohane 4:4), ndizosatheka kuti okhulupilira akhale ndi ziwanda. Okhulupilira akhoza kukhala muulamuliro wa ziwanda ndikumaoneka ngati ali ndi ziwanda. Ngakhale kuti ziwanda zikhoza kumulamuula munthu nachita machitidwe achilendo ngati chinyama (Luka 8:28-31), tisamuiwale Satana kuti akhoza kukhala ngati mngelo wa kuunika (2 Akorinto 11:13-15). Chinthu chofunika kwambiri kuti munthu udziwe ngati mzimu ukunama ndi kuona uthenga umene ukulalikidwa wa Uesu Khristu (1 Yohane 4:1-4).

Ndikofunika kwambiri kuti tidziwe za njira ndi machenjelero amene Satana amagwiritsa ntchito kuti "alikwire" okhulupilira (2 Akorinto 2:11). Amalonjeza kupeleka kutchuka, mphumi wa ndalama kapena chuma, mphamvu, udindo kapena zokondweretsa anthu. Okhulupilira ndi otchuka kale chifukwa ndi mwana wa Mulungu (1 Yohane 3:1), wapereka "Mwayi" ndi moyo wosatha (Aefenso 2:19-20), "Mphamvu" chifukwa ali mu mgwirizano ndi Ambuye mwini (Aroma 8:1-2). "Zosangalatsa" komanso mtendere wa nthawi za nthawi (Afilipi 4:7).

Tidzikhala osamalitsa pamene tiphunzira njira zomwe Satana amagwiritsa ntchito, chifukwa tikaphunzira kwambiri za iye kuposa mmene tiphunzilire za Mulungu, ndiye kuti pamenepo Satana watigonjetsa. Satana wakhala akugwiritsa ntchito njira zabodza kwa zaka zikwi zikwi. Njira yomugonjetsera ndi yodziwa choonadicho kuti tikakhonze kuzindikira njira zake zabodzazo.

Ngati sitimudziwa Satana kapena ziwanda pa moyo wathu, tidzavulala pa nkhondo yolimbana pakati pa Mulungu ndi Satana. Mtumwi Paulo akuchenjeza kuti

> ***Pakuti nkhondo yake siyolimbana ndi thupi ndi mwazi, koma yolimbana nawo maukulu ndi maulamuliro, amphamvu za kumidima, mizimu yoipa, ziwanda za mlengalenga, choncho; Dzitengereni nokha zida za Mulungu, Kuti muthe kugonjetsa zoipa za masiku ano, ndipo mutapanga zonse, muzatha kuima chiimire*** (Aefenso 6:12-13).

Zoyenera kuchita aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Mutu 6, Gawo 2

1. **Werengani nkhanizi ndipo tchulani maonekedwe a Angelo:**
   a. 1 Petro 1:12
   b. Luka 2:13
   c. Yuda 6

2. **Werengani Luka 24:4. Kodi angelo angatenge maonekedwe a munthu?**

3. **Werengani Ahebri 2:6-7. Kodi Munthu ndi muyeso wapamwamba kapena wapansi?**

4. **Werengani Masalimo 148:2-5. Anapanga (analenga) angelo ndi ndani?**

5. **Luka 20:35. Kodi angelo ali ndi ana?**

6. **Aefenso 6:12. Kodi angelo a Satana ali ndi ndondomeko komanso maudindo?**

7. **Werengani Chibvumbulutso 12:7. Kodi ngelo uti yemwe ali Kazembe wa gulu la nkhondo la Mulungu?**

8. **Kodi ndi gulu liti la angelo lomwe latchulidwa mowirikiza mu Baibulo? Akerubi? Aserafi?**

9. **Werengani Ahebri 1:14 Kodi ntchito yeniyeni ya angelo ndi yotani?**

10. **Werengani Chibvumbulutso 12:7-9. Kodi Satana ndi ndani?**

11. **Werengani Mateyu 25:41. Mathero a Satana ndi wotani?**

12. **Werengani Yesaya 14:12-14. Kodi Tchimo loyamba la Satana linakhuza chiyani?**

13. **Kodi dzina loti Satana limatanthauzanji?**

14. **Nanga udindo woti M'dierekezi umatanthauzanji?**

15. **Nanga mawu oti Njoka amatanthauzanji?**

16 **Werengani 2 Akorinto 11:13-15. Kodi amithenga ake a Satana amagwiritsa ntchito chiyani ponyenga?**

17. **Werengani 2 Akorinto 4:4. Kodi Satana ndi amithenga ake amafuna akwaniritsenji?**

18. **Tchulani maudindo kapema mayina awiri a angelo a Satana?**

19. **Werengani 1 Yohane 4:1-4. Ndi njira iti yodziwira mzimu kuti ndi woona kapena wabodza.**

20. **Werengani Aefenso 6:12-13. Nkhondo ya okhulupilira ndi yolimbana ndi ndi chiyani?**

Gawo 3
Munthu (Chiphunzitso cha munthu-Anthropology)

A. Chilengedwe cha Munthu

Chilengedwe cha munthu chinakonzedwa ndi Mulungu Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera (omwe amatengedwa kukhala Mulungu). Chikonzerochi chinaonetsedwa ku vesi yomwe imati, ***"tipange munthu mchifaniziro chathu monmga mwa chikhalidwe chathu"*** (Genesis 1:26). Utatu onse woyera unatenga mbali mchilengedwe cha munthu.

Chikonzerochi chinakhuza kupanga munthu "mchifaniziro" ndinso "mchikhalidwe" cha Mulungu. Mau awiri a mchifaniziro, "TSELEM" omwe ndi a chi Hebri komanso "EIKON" omwe ndi a chi giliki amatatnthauza maonekedwe a munthu. Mau awiri a chikhalidwe, "DEMUTH" mu chi Hebri ndi "HOMOIOSIS" mu giliki amatanthauza za chikhalidwe cha munthu. Mau oti maonekedwe ndinso chikhalidwe chamunthu amagwiritsidwa ntchito osati mwachindunji ndipo sayenera kugwiritsidwa ntchito mosindika. Chikonzero cha Mulungu chinali kupanga munthu, mmaonekedwe ndinso mchikhalidwe. Munthu azakhala wa moyo, wanzeru, wamakhalidwe abwino ndinso azakhala ndikuthekera kosankha, ngati Mulungu koma osakhala Mulungu. choncho adzakhala ndi kuthekera kocheza ndi Mulungu.

Mulungu Atate mwini anapanga munthu oyamba Adamu. Tinauzidwa kuti iye ***"anaumba munthu ndi dothi lapansi, nauzira pweya wa moyo mphuno mwache, munthuyo nakhala wa moyo"*** (Genesis 2:7). Mau atanthauzilidwa "kukhala" ndi a chi Hebri "NEPHESH" omwe amatanthauza "MZIMU". Mulungu anapanga thupi la munthu kuchokera ku zinthu zomwe adali atazipanga kale-dothi la munthaka. Adapanga mzimu wa munthu (mbali ya munthu yomwe siyakuthupi) osachokera ku chinachilichonse (Genesis 1:27). Kenako anaphatikiza ziwiri kukhala munthu.

Ophunzira akumbukire kuti Adamu adali amalengedwa mwapadeladera. Sanabadwe momwe munthu m'mene ayenera kubadwira. Anapangidwa ngati mamuna wamkulu amene analengedwa ndi nzeru. Mulungu anamusiya iye m'munda namupatsa ulamuliro oti atche zinyama maina (Genesis 2:8, 19).

Mulungu ananena kuti, ***"sikwabwino kuti munthu akhale yekha"*** (Genesis 2:18), kotero anaganiza kuti amupangire nzake omuthandizira. Adzatchedwa "mkazi" chifukwa adzachoka mwa mamuna (Genesis 2:18-23) ndipo dzina lake lizakhala "Hava" chifukwa ndi ***"mayi wa zamoyo zonse"*** (Genesis 3:20). Zinanenedwa kuti Mulungu adaumba mzimayi, kutanthauza kuti anagwiritsa ntchito zipangizo (nthiti ya Adam) ndikupanga thupi la mzimayi ndikulipatsa moyo (Genesis 2:21-23). Mamuna ndi mzimayi anali zotsatira za chilengedwe cha chionekere, chapaderadera komanso cha pompopompo. Sanachokere ku zolengedwa zina.

Mulungunso anapanga nyama ***"kuchokera ku nthaka"*** nadzipatsa moyo (Genesis 2:19). Nyama sizili ***"m'chifaniziro cha Mulungu"*** Ngakhale palibe amene angasutse kuti nyama zili ndi moyo komanso zimatha kuganiza, koma zilibe kuthekera kopanga chiganizo chabwino. Ndi zamoyo koma zilibe kuthekera kolingalira (2 Petro 2:12; Yuda 1:10).

B. Kuchimwa kwa Munthu

Adam ndi Hava amene Mulungu anawalenga ankakhala m'munda wa Eden (Genesis 2:10, 15). Ntchito ya mamuna inali kulima m'mundamo ndinso kuwuyang'anira (Genesis 2:15). Mulungu anauza mamunayo kuti atha kudya chipatso chilichonse cham'mundamo kupatula, cha ***"mtengo wakudziwitsda chabwino ndi choipa"*** womwe unali pakati pa mundawo moyandikana ndi "mtengo wa moyo" (Genesis 2:16). Adam adachenjezedwa (Mulungu asanalenge Hava) kuti akadya chipatso cha mtengo wodziwitsa zabwino ndi zoipa adzafa ndithu (Genesis 2:17) kuwonetsa kuti chilango chakusamvera kwake chizakhudza thupi lake ndinso mzimu wake (malemba a mu chi Hebri amanena mobwereza mauwa kuti "kufa, udzafa ndithu").

Njoka, (mokhala kapena kuti inalowedwa ndi Satana) (Chivumbulutso 12:9) inakwanitsa kumufikira mamuna kudzera mwa mkazi. Inamunyenga Hava (2 Akorinto 11:3; Timoteo 2:14) kuti adye chipatso choletsedwacho. Hava anampatsako china Adam ndipo iyenso anaswa lamuro la Mulungu (Genesis 3:6).

Tiyeni tiunike mwa mwatsatanetsatane zomwe zinapangitsa kuti munthu achimwe. Ziwani kuti njoka inamupeza mkazi yemwe sanali ndi mamuna nthawi imeneyo. Mamuna anali ndi ulamuliro m'mundamo chifukwa amasunga (kulondera) iwo (Genesis 2:15). Mamuna ndi mkazi anauzidwa onse kuti asazadye chipatso cha mtengo umenewo (Genesis 3:1). Chinjokacho chinagwiritsa ntchito mmodzi mwa iwo yemwe chinamuona kuti sangavute.

Mdyerekezi adayamba kuyankhura pofunsa funso lomwe limakhuza zomwe Mulungu samafuna. Chinjoacho chidafunsa ngati Mulungu adawauza kuti asadye chipatso cha mtengo uliwonse m'mundamo

(Genesis 3:1). Ili linali funso losakhala bwino chifukwa ngati samayenera kudya zipatso za m'mundamo amayenera kuwusiya mundawo ndi kukasaka chakudya. Funsolo limayamba kubweretsa kugalukira pa chifundo cha Mulungu. Funsolo limafunsidwanso kuti aone m'mene mzimayiyo amadziwira komanso kumvera malamuro a Mulungu.

Yankho la mkaziyo litipatsepo phunziro (Genesis 3:2-3). Ankafuna kukonza funso la chinjokacho kenako ndi kuyankha. Vuto linali loti amagwiritsa ntchito mau amene sanali mbali ya lamuro la Mulungu ndipo adaonjezera pa ilo. Adaonjezera kuti "usachigwire." Anthu ena amayesa ngati kuti Adamu adaonjezera lamulolo m'mene amamuuza Hava. Kaya ndi Adam kapena Hava adaonjezera lamulolo koma zosatira zake zinali zofanana, amaonjezera mau a Mulungu choncho amakaikira kufunikira kwake. Satana anatengelapo mwayi pa kuonjezelapo kwa lamulolo nanena motsutsana ndi chilango cha Mulungu (Genesis 3:4) ndi zolinga zake (Genesis 3:5). Anapereka "nzeru ya chabwino ndi choipa" ngati china chake chimene Mulungu amabisa chomwe ndichofunikira kuti iwo adziwe.

Kumbukirani kuti "zabwino" zinatanthauzilidwa kale kuti ndi zomwe Mulungu amachita (Genesis 1:4, 10, 12, 18, 21, 25, 31; 2:9, 12). Mtundu wa zabwino zomwe ndizosafunikira kudziwa ziyenera kukhuzana ndi zinthu zomwe Mulungu satengako gawo koma sizoipa mwa izo zokha kwa ena. Mwachitsanzo, munthu akhoza kumupatsa nzake amene ali ndi ludzu chakumwa ndicholinga chakufuna kuzindikirika ngati wothandiza m'malo mongomupatsa nzake waluzuyo chakumwa chifukwa ndi chikhumbokhumbo cha Mulungu (Marko 9:41). Ndikuchita "zabwino" komwe kumapangitsa kuti Mulungu asamaonekele. Monga takamba kale kuti mdyerekezi amapanga lamulo mdziko muno lomwe silizawerengera Mulungu konse.

Njokayo inanamiza mkaziyo pogwiritsa ntchito maonekedwe komanso kaganizidwe kake namusocheletsa (Genesis 3:6). Pamenepo Hava anasiya kuyenda mchikhulupiliro. Anasiya kukhulupilira Mulungu nayamba kuzikhulupilira yekha. Mdyerekezi anamuuza kuti adzakhala wa nzeru ngati Mulungu (Genesis 3:5). Ngati adzakhale wa nzeru ngati Mulungu sadzamadaliranso Mulungu pa moyo wake ndipo mwa icho adzapanga malamuro ake. Satana amamupatsa iye umulungu womwe iye mwini amaufunisitsa ataupeza (Yesaya 14:12-14). Tikuziwa kuti ***"wopanda chikhulupiliro sikutheka kukondweretsa iye"*** (Ahebri 11:6). Hava sanakhulupilire Mulungu pamene anadya chipatso cholesedwa. Mdyerekezi anamunamiza iye kuti Mulungu ndi oipa ndipo sakufunikira pa iye. Atha kusangalala ndi moyo popanda chikhulupiliro (2 Akorinto 11:3). Iye anadya chipatso.

Malemba anati ***"ndipo anapatsako mamuna wake ndipo iye anadya"*** (Genesis 3:6). Sitinauzidwe zimene awiriwa anakambirana Adam asanadye. Komanso sitinauzidwe maganizo a Adam kupatula kuti sananyengedwe nawo ndi chinjoka (1 Timoteo 2:14). Adam anapanga chisankho chake nachimwa. Malemba amatiuza "ndipo iye anadya" (Genesis 3:6). Onse anachimwa koma zilango zizakhala zosiyana.

Adam ndi Hava anazindikira kuti anachimwa ndipo anakhala ndi mantha. Anachita manyazi chifukwa anali maliseche (Genesis 2:25 cf. 3:7). Anasoka masamba a mitengo naziphimba nawo (Genesis 3:7). Anayesesa kuzibisa kwa Mulungu (Genesis 3:8). Uku kunali kuyesa koyamba kwa munthu kuti adzipulumutse yekha.

C. Zilango za Kuchimwa kwa Munthu

Njoka ndiyo inayamba kulandira chilango. Idzadya dothi masiku onse a moyo wake (Genesis 3:14). Chinjoka sichinali mdyerekezi koma mdyerekezi anali mwa chinjoka ((Satana amayendayenda dziko lapansi [Yobu 1:6; 2:1] komanso kunka kumwamba nakazenga milandu abale (Chivumbulutso 12:10). Chinjokacho ngati chida cha mdyerekezi chinaikidwa ngati chinyama chokanidwa pa dziko lapansi (Genesis 3:14).

Poti mdyerekezi ndi amene anachipatsa chinjoka mphamvu kuti chiyankhure nayenso analandira chiweruzo. Pazakhala udani waukulu kwambiri pakati pa iye ndi mbewu mzimayi (Genesis 3:15). Uwu ndi umboni wayamba mu Genesis kupita kwa mpulumutsi. Zimangotanthauza za kubadwa kwa paderadera kwa mpulumutsi, chifukwa tikamakamba za "mbeu" imachokera kwa mwamuna (Genesis 12:7; 22:17, 18). Mpulumutsiyu adzabadwa kwa msikana osamudziwa mamuna ndipo izi zinaikidwa bwino lomwe mu buku la Yesaya 7:14. Uwu ndi uneneri omwe mauneneri onse a mpulumutsi anachokelapo (Chivumbulutso 12:4-5). Njoka idzalalira chitende cha mpulumutsiyu koma mpulumutsiyu adzaphwanya mutu wa chinjokachi.

Chilango choyamba cha tchimo ndi chikumbumtima ("manyazi ndi umaliseche" Genesis 3:7) ndi kutha kwa kucheza kapena chiyanjano ndi Mulungu (anazibisa Genesis 3:8).

Mkazi analonjezedwa ***"masautso pobeleka"*** (Genesis 3:16) ndipo kuti adzakhumbira kulamulira mamuna wake komanso adzakhumbira kulamulilidwa ndi mamuna wake. Awa ndi mayeso amene Hava anakumana nawo pamene anafuna kuti alamulire Adam (ndichipatso) koma anafunanso anakamuletsa penapake.

Ndipo Mulungu anadzuzura Adam pomvera mkazi (Genesie 3:17). Ndizachiziwikire kuti Adam sanayenera kumumvera mkazi wake. Mamuna amene samamvesetsa ndimeyi amaganiza kuti munjira iliyonse sayenera kumvera mkazi wake. Uku ndikusagwiritsa ntchito bwino mau chifukwa Mulungu pa nthawi inayake adauzapo Abraham kuti ayenera kumvera mkaziwake Sarah (Genesis 21:12). Tigwiritse ntchito nthawi zonse zomwe Mulungu wanena kukhala muyeso wa chivomelezo chathu ku china chili chonse. Kuchimwa kwa Adam sikunachokere posatira ganizo la mkazi wake koma podya chipatso choletsedwa. Thembelero la Adam linakhuzana ndi kufunikira kokhetsa thukuta, kuti munthu apeze chakudya (Genesis 3:17-19).

Chilango chenicheni podya chipatso choletsedwa sichinaiwalidwe. Adam atachimwa adafa mu uzimu poti adasiya kucheza ndi Mulungu. Imfa yake yakuthupi idachitika patatha zaka 930 (Genesis 5:5). Yehova Mulungu anawonetsa chifundo kwa Adam ndi Hava powapangira zovala kuchokera ku zikopa nawaveka (Genesis 3:21). Kukhala ndi chikopa cha nyama kunafunikira kuti nyama yosalakwa iphedwe ngati nsembe. Ichi ndi chithunzithunzi chachiwonekere chakufunikira kwa nsembe kukuchotsa machimo komwe kunakwaniritsidwa ndi mpulumutsi (Ahebri 10:10, 12).

Adam ndi Hava adavekedwa ndi Mulungu nathamangisidwa m'munda wa Eden (Genesis 3:22-24). Izi zinayenera kuchitika powopera kuti ***"pokhapokha adatambasura dzanja lake ndi kutenga mu mtengo wa moyo nadya ndikukhala moyo mpaka muyaya."*** ndikosavuta kuzindikira chifukwa chimene Mulungu anachitira izi atazindikira kuti munthu wachimwa ndipo sikwabwino kukhala mpaka muyaya mu uchimo, ndithembelero. Imfa ya okhulupilira idzakhala chinthu chabwino chifukwa adzaukitsidwa ndi thupi lina lomwe lidzakhale la mgwiro ngati mpulumutsi, Yesu Khristu (1 Yohane 3:2) natengeredwa kumwamba komwe kuli mtengo wa moyo ndikopanda thembelero (Chivumbulutso 22:2-3).

D. Mapangidwe a Munthu

1. Thupi

Thupi la munthu lidayamba pamene Mulungu anapanga Adam kuchokera ku nthaka mchifaniziro chake (Genesis 1:26) kenako napanga Hava kuchokera kwa iye (Genesis 2:7, 21). Adam ndi Hava anagonana nabala ana. Ana oyamba awiri anali Kaini ndi Abele (Genesis 4:1, 2). Mitundu yonse ya anthu inachokera mwa Adam ndi Hava. Dzina la Hava limathanthauza ***"mayi wa za moyo zonse"*** (Genesis 3:20).

Thupi ndi mbali ya munthu. Lili ndi ziwalo, zowonera, kukhuzira, kumvetsera, kulawira ndi kununkhizira. Tonse timadziwa ziwalo za munthu monga mutu, manja ndi mapazi. Ndizofunika kudziwa kuti zili ndi ntchito zosiyanasiyana. Sitimayendera manja kapena kudyera mapazi. Matupi athu anapangidwa kuti atizindikiritse za thupi la uzimu lotchedwa "tchalitchi' "thupi la Khristu" (Aroma 12:4-5). Okhulupilira onse ndi mbali ya thupi la uzimu limeneli ndipo onse ndi ofunika koma amagwira ntchito zosiyana pathupi (1 Akorinto 12).

Thupi ndi chinthu chabwino, linapangidwa ndi Mulungu kuti likhale nyumba ya munthu wa mkati amene ndi osaoneka ndi maso. Ambuye Yesu anapeleka thupi lawo kuti likhale nsembe ya machismo athu (1 Akorinto 11:24) natiyanjanitsa ife ndi Atate kuti tikhale ***"oyera opanda tchimo ndinso manyazi"*** (Akolose 1:21-22). Ambuye Yesu analipira dipo la machimo athu mu thupi limeneli (1 Petro 2:24).

Momwemonso i\monga "omutsanza Yesu", (1 Akorinto 11:1) thupi lathu lipelekedwe kwa Mulungu ngati nsembe ya moyo kuti aligwilitse ntchito moyenera ndi chifunuro chake (Aroma 12:1-2). Yesu akuyenera kukwezedwa m'moyo wathu kudzera mgawo lililonse la moyo mpakana imfa (Afilipi 1:20).

Tiyenera kuchita china chili chonse chakuthekera kuti ndimatupi athu tikhale okonzeka kutumikira Mulungu (1 Akorinto 9:27), podziwa kuti tsiku lina tidzayankha kwa Mulungu malingana ndi zochita zathu (2 Akorinto 5:10). Chiwalo china chachin'gono cha thupi lathu, chotchedwa lilime, chiyeneranso kuteteza zoyankhura zathu (Yakobo 3:2-5). Matupi athu agwiritsidwe ntchito potengera uthenga wa imfa ya Yesu Khristu pamachimo athu kuti tikhale ndi moyo (2 Akorinto 4:10).

Tsiku lina thupili lizasandulika latsopano lomwe silizalawa imfa (1 Akorinto 15:40-44). Lidzakhala ngati thupi loukitsidwa komanso lokwezeka la Yesu Khristu (Afilipi 3:20-21). Thupi losandulikalo lizatilola kukhala ndi ubale onse ndi ambuye Yesu Khristu (2 Akorinto 5:6-8).

2. Moyo/Mzimu

Mzimu ndi mbali yosakhuzika ya umunthu. Siyingaonedwe, kukhuzidwa, kumvedwa, kulawidwa kapena kununkhizidwa. Thupi silingakhale opanda mzimu (Genesis 35:18), mau a chi Hebri "NEPHESH" ndi achi Greek "PSUCHE" satanthauzilidwa ngati mzimu koma "moyo" kapena munthu.

Adam atalengedwa Baibulo limati ***"ndipo yehova Mulungu amaumba munthu ndi dothi lapansi, nauzira mpweya wa moyo mphuno mwache, munthuyo nakhala moyo"*** (Genesis 2:7; 1 Akorinto 15:45). Sizili mkati mwa phunziloli kuwona mau onse ogwiritsa ntchito kufotokoza moyo ndi tanthauzo lake. Tiyeni tikhulipilire kuti Mulungu analenga mzimu wa Adam ndi Hava kudzera mu mpweya ndipo mzimu unapatsidwa kumtundu onse wa anthu (Eksodo 1:5). "NEPHESH" amagwiritsidwa ntchito pa moyo wa zinyama (Genesis 1:20, 21, 24, 30; 2:19).

Pamene tiyang'ana chimene mzimu uchita kuthupi, tiyenera tizindikire kuti Mulungu ali ndi mzimu (Mateyu 12:18; Ahebri 10:38) ndipo kuti munthu analengedwa mchifaniziro chake (Genesis 1:26-27).

Tiyeneranso kuzindikira kuti mu mzimu wa munthu muli kuthekera kopanga ziganizo zolondora. Izi zikutanthauza kuti mumzimu muli malo amene zisankho zimaunikidwa zisanakhazikisidwe. kuthekera kosankhaku kumatchedwa chifuniro cha munthu. Pokhala kuti mumzimu ndi momwe ziganizo nzimapangidwa, tiyenera kusendera kuti mzimu uyenera kupulumutsidwa (Masalmo 33:18-19; Machitidwe 2:41; Ahebri 10:39; Yakobo 1:21; 1 Petro 1:8-9) ndi kuchilitsidwa ku uchimo (Masalmo 41:4). Yesu sanangotifera, komanso anatipatsa mzimu wake natiombola ku machimo (Mateyu 20:28; Marko 3:4; Yohane 10:11, 15, 17; 15:13) ndinso kukhala ***"m'busa oyang'anira wa moyo"*** (1 Petro 2:25). Ngati kudzera mukusakhulupilira mzimu sudzaomboledwa, udzaonongedwa kujahena (Mateyu 10:28; 16:26).

Zina mwaziganizo zomwe munthu amayenera kupanga ndiko kukonda Mulungu (Deutronomo 6:5; 10:12-13; 30:6) kudzipeleka yekha kwa Mulungu pamene tichita cholondora (1 Petro 4:19) ndi kupereka miyoyo yathu chifukwa cha abale (1 Yohane 3:16). Mumzimu kapena mmoyo wamunthu ndi momwe mumakahala nkhondo yolimabana ndi makhalidwe oipa a dziko la pansi (1 Petro 2:11) komanso ndi momwe a phunzitsi onyenga amamukolera munthu osakhazikika mu uzimu (2 Petro 2:12-14).

Kuwonjezera kukhala malo omwe ziganizo zimapangidwa, mmoyo ndi malo amenenso za ku thupi zimapangidwa. Mzimu ukhoza kukhala wachisoni (Yobu 30:25), wovuta (2 Mafumu 4:27) wa chisoni chachikulu (Masalmo 43:5; Yeremiya 13:17; Mateyu 26:38) wolaswa (Luka 2:35), wa masautso (Aroma 2:9) ndi odana (2 Samueli 5:8). Utha ku khalano okonda (Nyimbo ya Solomo 1:7; 3:1-4), kukweza Ambuye (Luka 1:46) ndi wachikondwelero (Luka 12:19).

3. Mzimu wa Umunthu

Mau a mzimu ndi "RUACH" mu chi Hebri ndi "PNEUMA" mu chi giriki. Uwu ndi mutu wovuta kuphunzira chifukwa mau onse amagwiritsidwa ntchito kambirimbiri ndipo amatanthauza mphepo, kupuma kapena mpweya, Mzimu Woyera, mizimu yoyipa ndi mzimu wa umunthu kutengera ndi m'mene mauwo agwirittsidwira ntchito.

Mzimu wa munthu ndi mphamvu ya moyo wa uzimu ndipo uli mbali imodzi yosakhuzika ya munthu yomwe imachokera komanso kupangidwa ndi Mulungu (Mlaliki 12:6-7; Zekariya 12:1; Ahebri 12:9) makamaka ndi Mzimu Woyera (Yohane 3:6; 6:63). Mzimu wa munthu ndi ofunikira pa moyo (Luka 8:55; Yakobo 2:26).

Kolingana ndi mfundo zakatanthauzidwe ka mawu zomwe taphunzira mmbuyomu titenge ndime yachimvekere ndikuigwiritsa ntchito popeza zoona zenezeni za mzimu wa umunthu. Tikayang'ana mzimu wa munthu tiona kuti zitakataka zambiri za mzimu wa munthu ndi moyu (mtima) ndi zofanana. Tiyenera kudziwa kuti mzimu wa munthu ndi wosiyana ndi moyo wa munthu komanso mzimu (Ahebri 4:12).

Tikaona ndime zokhuzana ndi mzimu wa umunthu, timapeza kuti zili ndi kufunika kusanu:

a. Kulandira Uthenga

Mzimu wa munthu utha kulandira uthenga womwe umabwera monga chisomo (Agalatiya 6:18; Philimoni 1:25), zowona za chikhalidwe (Malaki 2:15-16) ndi vumbuluso (Aefeso 1:16-17) Uthanso kukwiyitsidwa (Machitidwe 17:16) ndi kutakasidwa (1 Mbiri 5:26; Ezara 1:1, 5).

b. Kusanthula kapena kuwunikira Uthenga

Mzimu wa munthu uthanso kuwunikira uthenga womwe walandira. Utha kuvomereza zowona za nthani (Yobu 6:4), kuziwa maganizo athu (1 Akorinto 2:11), kulingilira modzama (Masalmo 77:6), kumvetsetsa (Yobu 20:3; 32:8) ndikukhara wanzeru pokhuzana ndi ndi kuwunikira komanso kusanthula (Eksodo 28:3; Deutronomo 34:9; Aefeso 1:16-17).

c. Kuchita Chisankho

Pamene mzimu (wa munthu) walandira ndi kuunikira uthenga utha kusankha njira yoyenera kutenga. Ukhoza kusankha kusogoleledwa ndi Mzimu Woyera (Machitidwe 20:22 -23), kuzipeleka kwa Mulungu (Masalmo 31:5), kukhala ndi chukhulupiliro (2 Akorinto 4:13-14), kulapa machimo (Yesaya 57:15; 66:2) kapena kuukira Mulungu (Yobu 15:13) komanso kukhala osakhulupilika pamaso pake (Masalmo 78:8).

d. Kuyankha

Pamene chinthu chalandilidwa, kuunikidwa ndinso chisankho, kupangidwa, mzimu wa munthu umayankha kapena kuchita munjira zambiri, ingakhale zachimo.

Mzimu wamunthu ukhoza kufotokozedwa munjira zingapo popeza:

- Utha kukwiyitsidwa. Oweruza 8:3; Mlaliki 7:9; 10:4
- Utha kukwiyitsidwa munthawi yochepa. Miyambo 14:29
- Utha kuzunzidwa. Yobu 7:11
- Utha kukhala wamwano. Masalmo 76:12; Miyambo 16:18; Maliki 7:8
- Utha kuswedwa. Masalmo 51:17; Miyambo 15:13; 17:22; 18:14; Yesaya 65:14
- Utha kukhuzumutsidwa. Miyambo 17:27
- Utha kukakamiza. Yobu 32:18
- Utha kuphwanyidwa. Masalmo 34:18; Miyambo 15:4
- Utha kukhala onyenga. Masalmo 32:2
- Utha kudetsedwa. 2 Akorinto 7:1
- Utha kukhumudwitsidwa. Eksodo 6:9
- Utha kukhala okhuzidwa. 1 Akorinto 5:3-5; Akolose 2:5
- Utha kulakwitsa. Yesaya 29:24
- Utha kumva mphamvu ya ambuye. 2 Timoteo 4:22
- Utha kuzilongosora. Miyambo 29:11
- Utha kukomoka. Masalmo 77:3; 143:7; Yesaya 57:16; 61:3; Ezekieli 21:7
- Utha kukhala okhulupilika kwa munthu. Miyambo 11:13
- Utha kukhala ndi chikhumbokhumbo chachikulu. Machitidwe 18:25; Aroma 12:10-11
- Utha kukhala wopusa. Ezekieli 13:3
- Utha kukhala odekha. 1 Akorinto 4:21; Agalatiya 6:1; 1 Petro 3:4
- Utha kuperekedwa kwa ambuye. Machitidwe 7:59
- Utha kukhumudwa. Yesaya 54:6
- Utha kulimbitsidwa. Deutronomo 2:30
- Utha kukhala woyera. 1 Akorinto 7:34
- Utha kukhala ndi ulemelero. 2 Akorinto 12:18
- Utha kukhala wodzichepetsa. Miyambo 16:19; 29:23
- Utha kukhala wansanje. Numeri 5:14
- Utha moyo mchiffuniro cha Mulungu. 1 Petro 4:6
- Utha kukhala wokhulupirika. Numeri 14:24
- Utha kukhwimitsidwa. Ahebri 12:23
- Utha kulimbitsa ena. Eksodo 35:21; Miyambo 16:2; Chibvumbulutso 19:10
- Utha kusunthidwa. Yohane 11:33
- Utha kupangidwa kukhalanso watsopano. Ezekieli 11:19; 18:31; 36:26
- Utha kuponderezedwa. 1 Samueli 1:15
- Utha kugonjetsedwa. Masalmo 142:3; 143:4
- Utha kukonzekera. Machitidwe 19:21
- Utha kukhala osauka. Mateyu 5:3
- Utha kupemhera. 1 Akorinto 14:14-16
- Utha kusungidwa. Yobu 10:12; 1 Atesalonika 5:23

- Utha kukhala bata. 1 Petro 3:4
- Utha kukhala ndi maonekedwe a mtundu wa khungu. Yesaya 19:3; Yeremiya 51:11
- Utha kupatsidwanso mphamvu zatsopano. 2 Akorinto 7:13
- Utha kukondwa. Luka 1:47
- Utha kukonzedwa mwatsopano. Aefeso 4:21-24
- Utha kufuna mpumulo. 2 Akorinto 2:13
- Utha bkudzutsidwanso. Genesis 45:27; 1 Samueli 30:12
- Utha kuzilamura wokha. Miyambo 16:32
- Utha kukhala osasangalala. 1 Mafumu 21:5
- Utha kufuna ambuye. Yesaya 26:9
- Utha kutumikira. Aroma 1:9
- Utha kupilira kumatenda. Miyambo 18:14
- Utha kudekha. Marko 8:12
- Utha kukhala okhazikika. Masalmo 51:10
- Utha kukhala wa mphamvu. Luka 1:80
- Utha kukhala chitsanzo cha ena. 1 Akorinto 14:31-32
- Utha kugonjera. Ahebri 12:9
- Utha kukhala wa manyazi ndi osalimba mtima. 2 Timoteo 1:7
- Utha kuzunzika. Genesis 41:8; Yobu 21:4; Danieli 2:1-3; Yohane 13:18-21
- Utha kukhala wosalamulilidwa. Miyambo 25:28
- Utha kulumikizana ndi ambuye. 1 Akorinto 6:17
- Utha kulumikizana ndi nosakhulupilira ena. Afilipi 1:27
- Utha kufooketsedwa. Yoswa 2:11; Oweluza 15:19; 1 Mafumu 10:4-5
- Utha kukhumba. Masalmo 51:10-12
- Utha kupembeza. Yohane 4:23
- Utha kuchitira umboni za chiombolo cha Khristu. Aroma 8:16

4. Mtima

"Mtima wa munthu ndi nkhani imene yaunikiridwa bwino mu Baibulo lonse. Liwu la chi Hebri lokuti "LEBH" komanso la chi Greek lokuti "KARDIA" agwiritsidwa ntchito pafupifupi kokwanira chikwi. Mauwa agwiritsidwa ntchito kwambiri kutanthauza chiwalo cha mkati mwa thupi chopopa magazi kuzera mu timisempha (2 Samueli 18:14; 2 Mafumu 9:24). M'malo mwake liwuli kawirikawiri likugwiritsidwa ntchito kusonyeza likulu la zichitichito mthupi la munthu.

Pamene tiunikira m'mene liwuli lagwiritsilidwa Baibulo, matanthauza anayi akuululika.

a. Likulu la Nzeru Kaganizidwe

Mtima ukuimira likulu la gawo lomwe limathandiza kuganiza mozama. Uli ndi kuthekera kowuunikira bwino ziganizo (Deutronomo 8:5), umayamikira (Masalmo 119:11) komanso kukonzekera mwakupanga madongosolo (Ahebri 4:12). Komanso mtima ukhoza kukhala gwero la maganizo ndi machitidwe a uchimo (Mateyu 15:19-20).

b. Likulu la Maganizo a Mphamvu a Mtundu Wina Uliwonse

Mtima umagwiritsidwa ntchito ngati likulu la maganizo a mphamvu a mtundu wina uliwonse. Utha kukonda (Deutronomo 6:5) kukhala ndi khumbo (Masalmo 37:4), kukondwa (Masalmo 104:15; Yesaya 30:29; Akolose 3:6) komanso mtima ukhoza kukhala wachisoni (Nehemiya 2:2; Aroma 9:2), woipa (Masalmo 73:21) komanso ukhoza kuzizuzula wokha (Yobu 27:6).

c. Likulu la Mphamvu ya Zofuna Munthu

Mtima ndi momwe mumachokera mphamvu ya maganizo a munthu kapena momwe mumachitika zisankho. Utha kufunafuna Mulungu (Deutronomo 4:29), utha kusinthidwa mmaganizidwe (Eksodo 14:5) kapenanso kuumitsidwa kwa Mulungu (Eksodo 8:15; Ahebri 4:7).

d. Kasupe wa Moyo wa Uzimu

Mtima ndi gwero la moyo wa uzimu. Mau a Mulungu akunena kuti "ndi mtima munthu amakhulupilira ndi kutengapo chilungamo" (Aroma 10:9-10). Kwa okhulupilira mtima ndi nyumba ya Ambuye Yesu (1 Petro 3:15; Aefeso 3:17) komanso ya Mzimu Woyera (2 Akorinto 1:22).

5. Chikumbumtima

Liwuli likupezeka mchipangano chatsopano chokha. Ntchito za chikumbumtima zikuperekedwa pogwwiritsa ntchito liwu lokuti "mtima" mchipangano chakale (1 Samueli 24:5; Yobu 27:6). Liwu la mchigiriki lakuti "SUNEIDESIS" limatanthauza mwa chindunji kuti "kudziwa ndi" kapena "kukhala ndi chinthunzithunzi cha iwe mwini." Limaimirira chizindikiro chochokera m'maganizo chomwe chimatidziwitsa kuti tikupanga zabwino kapena zoipa. Chikumbumtima ndi mbali ya munthu imene imamulamula kuchita zokhazo zomwe akuziwa kuti ndizabwino. Ndizotheka kuchita zinthu zoipa koma uli ndi chikumbumtima chabwino chifukwa choti wakhala ndi uthenga wosokonekera.

Chikumbumtima cha munthu wochimwa chikhoza kumutsogolera bwino (Yohane 8:9; Aroma 2:15), ngati munthuyo anaphunzitsidwa za muyeso wa Mulungu wa chabwino ndi choipa. Chikumbumtima chikhoza "kulochedwa" monga chitsulo chamoto (1 Timoteo 4:2) ngati munthu achimwa mobwerezabwereza.

Munthu akaphwanya mulamulo a Mulungu, chikumbumtima chake chimadetsedwa (Tito 1:5) komabe chikumbumtima chikhoza kuyeretsedwa ku uchimo (Ahebri 10:22). Chikumbumtima cha Khristu kudzera mu uthenga wa Mzimu Woyera chikuyenera kumulondolera kuchita za mgwiro m'moyo. Chikuyenera kumusogolera kumvera ulamuliro umene akutsatira (Aroma 13:5) kupilira bwanankubwa wopanda chilungamo (1 Petro 2:19), komanso kusaononga chikumbumtima cha m'bale wofooka (1 Akorinto 8:7, 10, 12).

6. Maganizo

Liwu la mchigiriki loyimira maganizo ndi "NOUS." M'maganizo ndi malo omwe mphamvu za kaganizidwe, nzeru komanso makhalidwe a mphamvu a mtundu wina uliwonse monga chikondi, chimwemwe, mtendere, mantha ndi udani zimakumanirana kuti munthu apange chiganizo. Liwuli limaimira ntchito zonse za ubongo komanso mzimu wa munthu, kotero ndipokumanirana magawo ofunika komanso osafunika a munthu. W.E. Vines anati:

> Maganizo ndipo pagona kuunika kwa chikumbumtima, kuphatikizirapo kukhala tcheru ndi kumvetsera, kukhuzika mu mtima, kuika mtima pa chinthu ndinso kuweruza. Mau ofanana nawo a mchigiriki ndi "DIANOIA" omwe akutanthauza kuti "kulingalira" komanso "ENNOIA" kutanthauza "ganizo, chikhulupiliro m'moyo wa munthu kapena lingaliro." Ngakhale maganizo ndi mtima zili zogwirizana koma ziwirizi ndi zosiyana (Ahebri 8:10, 16).[106]

Ngakhale ganizo la "mtima" likuoneka mu chipangano chakale, mulibe liwu lake la chi Hebri. M'malo mwake likulongosoledwa mbali ya mtima, moyo ndi mzimu chifukwa cha ichi tanthauzo lathu la maganizo likuchokera mu zilembo za chi Greek.

Anthu owombora ndi osaomboledwa onse ali ndi maganizo (Aroma 14:5). M'mene munthu amaganizira komanso m'mene amagwiritsira ntchito maganizo omwe Mulungu anampatsira zili zofunikira kwa iye mwini (Aefeso 4:17-18; Ahebri 4:12) pamene mawu oti ENNOI akugwiritsidwa ntchito komanso kumasulilidwa ngati "maganizo" ndipo tiyenera kufuna kuuziwa ichi (Aroma 11:34; 1 Akorinto 2:16) Mulungu anatipatsa ife maganizo ndi cholinga choti timkonde iye (Mateyu 22:37; Marko 12:30; Luka 10:27) ndikumudziwitsa iye (Luka 24:45). Maganizo a mkhristu anapangidwa kuti adziwe chowonachi chomwe chili mwa Atate ndi Mwana (1 Yohane 5:20) pamene DIANOIA akumasulilidwa kuti "kumvetsetsa."

Mtima womwe Mulungu anatipatsa utha kuganiza mwa nzeru. Izi zimatsimikizidwa podziwa kuti umatha kupeza mayankho a njira zina za masamu (Chivumbulutso 13:18) ndinso kumvetsetsa zotsatira za kuganiza mozama (Chivumbuluso 17:9). Kupyolera mu kuthekera kumeneku ndinso kumvetsetsa, mtima umaona njira zoyenera zomwe uzisata zomwe zimapangisanso kuti ukhale ndi chikumbumtima (Aroma 7:23, 25). Kukhwima maganizoku kumapangitsa kuti pakhale kuthekera kotsogolera ena (1 Akorinto 14:19) ndiponso kumapangitsa kapena kuthandiza anthu okhwima kwambiri kuti abweretse mgwirizano mwa Yesu Khristu (1 Akorinto 1:10). Mtima wayenera kukhala wachilungamo kwa iwo wokha, Mulungu komanso kwa anthu ena (2 Petro 3:1). Mtima wa munthu unapangidwa kuti uzigwira ntchito limodzi ndi mzimu wa munthu mu magawo onsewa (1 Akorinto 14:15).

Ngakhale mtima wa munthu ukhoza kugwiritsidwa ntchito pa ntchito ya Mulungu (Marko 12:30) ungathenso kupanga chisankho chopandukira Mulungu kapena osachita zinthu za uzimu moyenera (Aroma 1:28; 1 Timoteo 6:5; 2 Timoteo 3:18). Ungathe kukhala wa mwano kwa Mulungu (Akolose 1:21). Mtima umatha kuipitsidwa (Tito 1:15).

Ngakhalenso mtima wa okhulupilira umatha kukhala osapindura (1 Akorinto 14:14) pamene uli wouma mtima kapena ongoganiza zinthu za thupi zokha (Luka 1:51; Aefeso 2:3; Akolose 2:18). Umakhalanso otekeseka pamene ziphuzitso zabodza zikukhulupilidwa ngati zoona (2 Atesalonika 2:2) pamene NOUS atanthauzilidwa ngati "machitidwe."
Ndi chiyamiko, tinapeza kuti mtima wa munthu utha kusinthidwa kuti udziwe chifuniro cha Mulungu (Aroma 12:12), kusiya zichitichito zamachimo (Aefeso 4:22-24), kukhala okonzeka ku chirichonse (1 Petro 1:13), kukhala okonzeka ku mavuto osakuyenera (1 Petro 4:1) pamene ENNOIA akutanthauzilidwa ngati "cholinga" ndinso kusungidwa ndi mtendere wa Mulungu (Afilipi 4:7).

7. Thupi

Nthawi zonse mau oti "thupi" amaimira chinthu chomwe chimapanga maonekedwe a chamoyo, kaya ndi khungu lomwe limatchinga thupi (Genesis 2:21; Eksodo 12:8; Luka 24:39) kapena zina zonse zopezeka pa thupi (Genesis 6:17, 19; 1 Akorinto 15:39; Ahebri 5:7). Motengera mu Baibulo, mau oti "thupi" amaonetsa mgwirizano wa zowoneka ndi sozawoneka pa thupi la munthu.

Mulungu anasanduka munthu kupyolera mwa Yesu Khristu (Yohane 1:1, 14; 1 Timoteo 3:16) monga mbumba ya Davide (Aroma 1:3; 9:5). Izi zikutanthauza kuti Mulungu adasanduka munthu weniweni. Adapangidwa mchifanizo cha thupi la uchimo, koma thupi lake silidali lauchimo (Aroma 8:3). Adali "Mbuye" wa Davide komanso "Mwana" wa Davide (Mateyu 22:45). Yesu adabwera kudzatifera ife kuti apange mgwirizano pakati pa ife anthu ndi Mulungu (Aefeso 2:14- 15; Akolose 1:22-23) ndinso kuononga mphamvu za mdyerekezi (Ahebri 2:14). Mau a Mulungu amatiuza kuti kuzabwera aneneri onyenga amene adzanena kuti Yesu sanabwere m'thupi (1 Yohane 4:2; 2 Yohane 1:7).

Chipangano chakale chidaunika kufunika kwa Mulungu kubwera mu thupi. Chophimba cha likasa ndinso kachisi chinali chidziwitso kuti thupi la Yesu layenera kupereka moyo osatha wa Mulungu ku mtundu wa anthu (Ahebri 10:19-20; Mateyu 27:51). "Manna" amene adathandiza a yuda mchipululu kwa zaka makumi anayi chinali chidziwitso cha kuwomboledwa ndinso chokhalira moyo chomwe Yesu angabweretse kudutsa mu thupi lake, chimene chidzaperekedwa mwa chisomo ndi kulandiridwa ndi chikhulupiliro (Eksodo 16:31-35; Yohane 6:51-56). Masalmo a Davide ananenanso kuti thupi la mesaya silizaola ayi,zomwe zikusonyeza poyera kuuka kwa akufa kwa Yesu (Masalmo 16:10; Machitidwe 2:31) ndi mayankho a Mulungu ku mapemphero (Ahebri 5:7).

Masautso ndinso cholinga cha thupi la Yesu Khristu zinasanduka chitsanzo chabwino ku mtundu wa anthu kuti adzisatira (1 Petro 4:1-2). Thupi la munthu mu malemba limaoneka kuti ndi lamachimo kwambiri ndinso lomwe limakhala pa nkhondo yolimbana ndi mzimu oyera (Agalatiya 5:16-17). Mbali imodzi ya ntchito za mzimu woyera ndikusonyeza ndi ndikudziwitsa za vuto la machimo ndinso zotsatira zake (Yohane 16:8-11).

Pali ziziwitso zina za thupi zomwe zidafotokozedwa ndi mau a Mulungu,thupi lopanda mzimu ndi lakufa (Yohane 6:63), pakuti thupi limabereka thupi, Mzimu Woyera umayenera upatse thupi mzimu kuti thupilo likhale ndi moyo (Yohane 3:6). Timakonda kuzisangalira ndinso kuzinyadira pa thupi lathu (Aefeso 5:28-29), ndipo thupi litha kukhala ndi nzeru za kuya (1 Akorinto 1:26-29).

Thupi ndilofooka kumayesero (Mateyu 26:41), lisadapulumutsidwe, zochitika za thupi ndi chikhalidwe chenicheni cha munthu (Aefeso 2:3). Thupi limatenga gawo mu momwe mtima umaganizira (Akolose 2:18). Kuchita zokhumba za thupi zimaonetsa kusakonda mphamvu ya ulamuliro (2 Petro 2:9-10), akhristu amakula mu mzimu pophunzira kumvera omwe ali ndi ulamuliro pansi pano (Aefeso 6:5). Kuvomereza ulamuliro ndi nkhondo, popeza thupi limadana ndi malamulo a za uzimu (Aroma 7:5).

Moyo wathu wakuthupi ndi omwe uzaweruzidwa ndi ena, ngakhale sitiyenera kuweruza ena pa ntchito za thupi (Yohane 8:15). Sitiyenera kulemekeza ena kamba ka ntchito zawo za kuthupi (2 Akorinto 5:16) kapena kulemekeza zinthu za thupi monga: miyambo, umzika, ntchito, kapena kuzionetsera a chiyero, chibadwidwe (Afilipi 3:2-7). Nthawi yathu yamoyo tiyenera kukhala mu chifuniro cha Mulungu (1 Petro 4:6).

Thupi lili ndi zofooka zake. Thupi ndi lofooka pokana tchimo (Aroma 6:19) dziko limapereka ku thupi zinthu za uchimo (1 Yohane 2:16). Thupi palokha limadzetsa machimo ochuluka amene azamupangise

ochimwa kusalandira madalitso a muyaya (Agalatiya 6:8). Thupi lidzafota ndithu (1 Petro 1:24-25). Aphunzitsi onyenga azakaniza otsatira awo powauza zokhumba za thupi (2 Petro 2:18-19).

Thupinso lili nazo zofooka ku mbali ya zogonana. Ukwati ndi kukhala pamodzi pakati pa mamuna ndi mkazi nakhara thupi limodzi, kotero zilakolako za thupi zimahkala pa zinthu za "zachilendo" zomwe zili kugonana amuna okhaokha, akazi kugonana okhaokha ndinso kugonana ndi zinyama (Marko 10:8; Yuda 1:7). Tchimo lochita ukudziwa limazetsa chionongeko ku thupi (1 Akorinto 5:5).

Kufooka kwina nkokuti thupi lili pa mtetete kwakululu ndipo limakumana ndi kusintha kwambiri kwa zinthu (2 Akorinto 1:17) kumene kungadzetse kusakhazikika pa moyo wa munthu wokhulupilira. Ngati tisinthe maganizo kawirikawiri pongotengera zinthu zongochitika kwa kanthawi chabe, tikhoza kukhala anthu osokonezeka komanso osakhazikika.

Thupi lilinso ndi malire. Chochitika ku thupi (monga mdulidwe) sizimasonyeza uzimu (Aroma 2:28). Miyambo siyingakhoze zofooka komanso zolepheletsa za thupi (Akolose 2:23; 1 Petro 3:21).

Thupi silingakhale la chiyero posunga malamulo (Aroma 3:18) komanso thupi palokha silingathe kuchita zabwino. (Aroma 7:18). Komanso madalitso a Mulungu sanaperekedwe ku thupi ndi mwazi chabe (1 Akorinto 15:50). Thupi limafuna kuunikira kwa uzimu mwapaderadera (Mateyu 16:17).

Palinso nkhondo mu umoyo wa okhulupilira ndi thupi. Pamene munthu akhulupilira Yesu Khristu, amadziwa kuti Yesu anafera kulipira machimo ake (Agalatiya 5:24). Kumvetsetsa kwa mfundo iyi kumafuna kukula mu uzimu kwa okhulupilirayo. Okhulupilira amene sanakure mu uzimu amaona ngati ali wamuyaya ndinso wotetezeka mdzanja la Mulungu (Yohane 10:27-30) komanso kuti anamasutsidwa ndi Yesu Khristu (Agalatiya 5:1), Kotero mwa kusadziwa amafuna kupitiliza zokhumba za thupi. Chitetezo chathu mwa Khristu ndinso mtendere wake sizinapangidwe kukhala mwayi woti tizifunafuna za kuthupi (Agalatiya 5:13). Iyi ndi gawo la nkhondo.

Mbali ina yankhondo imadziwa kuti thupi lili ndi zofuna zake (Yohane 1:12-13) ndipo thupi ndi kukhazikika mu uchimo limachita nkhondo ndimaganizo (Aroma 7:25) ndinso Mzimu Woyera (Agalalatiya 5:16). Wokhulupilira ayenera kusankha uchimo wa thupi kapena zinthu za Mzimu Woyera (Aroma 8:3-13). Ndi mphamvu ya Mzimu Woyera zilakolako za thupi zingagonjetsedwe (Agalatiya 33:5; 5:16). Dziwani kuti nkhondo yeniyeni ya mzimu imene timakumana nayo simachokera ku thupi lathu (2 Akorinto 10:2-3), koma Satana ndi mphamvu yake (Aefeso 6:12).

Gawo la ulendo wathu wa uzimu ndikufuna kukhala woyeretsedwa ku uchimo wa thupi pakukhala woyera (2 Akorinto 7:1). Tiyenera kumufuna Yesu kuti akhale mu moyo wathu ndinso zikoka zathu zichoke (Aroma 13:14) kotero Yesu akawonetseledwe ku thupi lathu (2 Akorinto 4:11). Izi zingatheke kudzera mu moyo wokhulupilira Yesu Khristu (Agalatiya 2:20). Kotero kuti thupi lathu lizapelekedwe ku thupi la Khristu (Akolose 1:24).

Tiyeninso tizindikire kuti Mulungu amatikonda ndipo akhoza kutipatsa "Munga m'thupi" kuti tingazikwezeke tokha koposa (2 Akorinto 12:7).

8. Chikhalidwe cha Uchimo

Chowona chakuti uchimo wa Adam unapatsidwa kwa munthu aliyense zikufotokozedwa ndi mau oti "chikhalidwe cha uchimo." Izi zikutanthauza kuti munthu aliyense (kupatula Yesu Khristu amene analibe Atate wake pansi pano) analandira khalidwe la uchimo la Adam kutsatira chiweruziro (Aroma 5:12-14; 18-19).

Chikhalidwe cha uchimo ndi gawo la thupi ndinso lochititsa uchimo mmoyo wa munthu aliyense. Tiphunzira za "chikhalidwe cha uchimo" pa mutu 7, "Dongosolo la Mulungu."

9. Chifuniro

Pali mau awiri mu chi Greek amene amagwiritsidwa ntchito posonyeza zofuna za munthu. Mawu oyamba "THELEMA" omasonyeza "chikhumbokhumbo". Achiwiri "BOULEMA" kusonyeza ndondomeko kapena dongosolo. Onsewa amagwiritsidwa ntchito kwambiri ponenelera zokhumba kapena dongosolo la Mulungu, koma popeza munthu analengedwa mu chifanizo cha Mulungu (kusonyeza kuti munthu alinso naye ndi "zofuna"), amagwiritsidwa ntchito pofuna kunenelera zofuna kapena madongosolo a munthu.

Chifunilo cha munthu chimatha kukhala cha mphamvu kwambiri. Monga mmene munthu akhonza kusankha Mulungu, angathenso kusamusankha Mulungu (Yoswa 24:15) komanso ***"kupanga zokhumba za thupi ndi maganizo"*** (Aefeso 2:3). Zofuna za munthu zilibe mphamvu mwazokha

kugonjetsa chikhalidwe cha uchimo (Aroma 7:15-21). Mzimu Woyera umapereka mphamvu kupyolera mwa Khristu ya ***"kuchita zinthu zonse"*** (Afilipi 4:13).

Ngakhale zofuna za munthu zitakhala ndi mphamvu maka, sizingakhonze kumupulumutsa munthu (Yohane 1:12-13). Munthu ayenera kulandira mphatso ya Khristu pokhulupilira dzina lake (Yohane 1:12-13; Machitidwe 4:12), Pamene munthu akakhulupilira mwa Mwana wa Mulungu, Yesu Khristu, munthu ameneyo azakhala ndi moyo wosatha ndipo sazataika (Yohane 6:39-40).

Mulungu amafuna kuti chifunuro cha munthu chikhale ngati cha iye. Yesu anatiphunzitsa komanso anakhala mu umoyo umenewu (Yohane 5:30; 6:38, 39). Chifukwa chimene David anaitanidwa "munthu wa mtima wa Mulungu" (Machitidwe 13:22) ndi chakuti amafuna kuchita chifuniro cha Mulungu angakhale nthawi zina amalephera.

Chikhumbokhumbo chochita chifuniro cha Mulungu ndi chofunika kwambiri kuchimvetsa (Yohane 7:17). Mulungu sakufuna kungophunzira chabe kudziwa chifuniro chake koma akufuna moyo wosinthika. Munthu amene amewerenga mau a Mulungu pongofuna kumadziwa ndipo osakhala mu mau adzakhala ndi moyo wosokonezeka.

Mu mau a Mulungu timapeza kuti mtundu wa anthu utha kuchita zofuna zawo ndi cholinga choteteza (Mateyu 1:19) kuzenga mulandu mzake (Mateyu 5:40) komanso kufuna kubwereka kanthu kwa ena (Mateyu 5:42). Tipezanso kuti mtundu wa anthu utha kusankha kusata Khristu (Mateyu 16:24-25), kukhala wabwino (Mateyu 20:26-27), kukhala moyo wachiyero mwa Yesu (2 Timoteo 3:12), komanso kufuna kuti ena aziwapatsa ulemu wapaderadera (Mateyu 7:12).

Pamene "chifuniro" chapyora "chokhumba" chimakhala "chikonzero" mau a chi Greek "BOULEMA" amatanthauza "chokhumba chokhala chikonzero." Mau amenewa amatanthauzilidwa mu njira zosiyanasiyana, koma onse amakamba za chikonzero cha zokhumba. Mulungu ali ndi chifuniro chimene anakonza kale (Aroma 9:19), Mwana ali ndi ntchito yakeyake mu chikonzerochi (Mateyu 11:27).

Chikonzero chitha kuyambira kuchokera pa chikhumbokhumbo chofuna kuteteza ena (Machitidwe 27:43) kuwapweteka (Yohane 11:53; 52:10; Machitidwe 5:33), kapena kuziteteza wekha (Machitidwe 27:39). Patha kukhalanso makonzedwe a kayendedwe (Machitidwe 15:37), kupeza choonadi (Machitidwe 23:8) kuchita nkhondo (Luka 14:31) angakhalenso kuchimwa. Zokonzekera zitha kuchokera kwa Mulungu kapena ku thupi (2 Akorinto 1:17).

Zoyenera kuchita aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Mutu 6, Gawo 3

1. **Werengani Genesis 1:26. Munthu anapangidwa mu chifanizo chayani?**

2. **Werengani Genesis 2:7. Munthu anakhalanji atauziriridwa mpweya wa Mulungu Mfuno mwake?**

3. **Werengani Genesis 2:18. Chifukwa chiyani mkazi anapangidwa?**

4. **Werengani 2 Petro 2:12, Yuda 1:10. Kodi munthu amasiyana bwanji ndi nyama?**

5. **Werengani Genesis 2:16-17. Adamu analetsedwa chiyani?**

6. **Werengani Genesis 2:17. Chilango chake chinali chotani ?**

7. **Werengani Genesis 3:8-19. Miyoyo ya mkazi ndi mwamuna inasintha motani ataphwanya lamulo la Mulungu?**

8. **Werengani nkhaniyi ndipo mulembe za chilengedwe cha munthu.**
   a. Genesis 2:7
   b. Yakobo 2:26
   c. Aroma 10:9-10
   d. 1 Timoteo 4:2
   e. Aroma 12:2
   f. Genesis 2:21
   g. Aroma 5:12-14
   h. Yohane 1:12-13

Gawo 4
Mkangano wa Angelo

Zakuti pali nkhondo nkhondo pakati pa Mulungu ndi mdyerekezi zanenedwa kwambiri mundime za phunziro limeneyi. Nkhondoyi ikutchedwa kuti mkangano wa a ngelo. Tsatanetsatane wa mkanganowu ndiwaukulu kwabasi ndipo sizimene tikufuna kukamba makamaka mu phunziro la buku lathuli. Ngakhale zili choncho tilongosolakobe mochepa popeza zithandiza kuyankha funso limene limafunsidwa nthawi zonse "Chifukwa chiyani mtundu wa anthu ulipo?"

Munthawi imene munthu asanalengedwe, Mulungu anasankha kupanga mtundu wina wokhala ndi moyo. Amoyowo amatchedwa kuti angelo. Mfumu ya angelo anali Lucifer (woipa) amene anasankha kuyesa kulanda ufumu wa Mulungu (Yesaya 14:12-14). Lucifer anachimwa (Ezekieli 28:11-19) ndipo anatchedwa kuti woipa ndinso mdyerekezi (Chivumbuluso 12:9). Mdyerekeziyo adagamulidwa kupita ku moto wosatha womwe adamukonzera pamodzi ndi angelo womwe anali kumutsata iye (Mateyu 25:41).

Mdierekeziyo anadandaulira Mulungu pokhuzana ndi chigamulocho, nchifukwa chigamulocho sichinachitike. Chigamulochi chizachitika pakazadutsa zaka zokwana chikwi mu ulamuliro wa Yesu Khristu (Chivumbulutso 20:14). Munthu ali pakatikati ndipo ali ndi udindo pa zotsatira za mkangano wa pakati pa Mulungu ndi mdyerekezi.

Mtumiki Paulo adafotokoza bwino kuti mkanganowo umakhuza anthu okhulupilira. Adatero mu Aefeso 6:12, ***"Mu chilimbitso chathu sicholimbana ndi mnofu ndi magazi, koma kulimbana ndi ulamuliro, mphamvu, dziko la kum'dima, kulimbana pofuna kukaniza mzimu ofooka mu ufumu wa kumwamba."*** Nkhondo yeniyeni ya okhulupilira ndiyo yolimbana ndi satana ndi mphamvu zake, osati ndi ndi anthu. Kuti timenye nkhondoyi tiyenera ***" kuvala zida zonse za nkhondo za Mulungu, kuti muzathe kuletsa mdyerekezi mu nthawi ya zoipa; ndi kudzapanga chilichonse, kuti muzayime nji ."*** (Aefeso 6:13).

Zotsatira zonse za mkangano, komanso zoti ife okhulupilira nkumachita chiyani sizikudziwikiratu koma tsiku lina zizadziwika bwinobwino (1 Akorinto 13:12) pakadali pano zomwe tazizindikira ndizokwanira. Tiyende ndi ndichikhulupiliro (Ahebri 11:6) ndi kukonda Mulungu komanso kukonda wina ndi mzake (Marko 12:29-31).

Zoyenera kuzichita aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Mutu 6, Gawo 4

1. **Werengani Yesaya 14:12-14. Kodi tchimo lenileni la Satana ndi lotani?**
2. **Werengani Ezekiel 28:11-19. Kodi udindo wa Satana pachiyamba unali wotani?**
3. **Werengani Mateyu 25:41. Kodi nyanja ya moto inalengedwera ntchito yanji?**
4. **Werengani Chibvumbulutso 20:14. Satana ndi angelo ake azaponyedwa liti mu nyanja ya moto?**
5. **Werengani Yohane 16:11. Kodi chachitika kale kwa Satana ndi chiyani?**
6. **Popeza Satana waweruzidwa kale, mulandu wake watchulidwa. Kodi ife titani pamenepa?**
7. **Popeza Satana anali atagwa kale pamene amanyenga Adamu ndi Hava. Pamenepa tinganene zotani pa nkhani ya kugwa kwa Satana?**
8. **Popeza munthu ali pakati pa chiweruzo cha Satana ndi kukwaniritsidwa kwa chiweruzo chake, tinganene chiyani za kupezeka kwa munthu?**
9. **Werengani Aefenso 6:10-18. Kodi Mkhristu achitenji kuti agonjetse machenjerero a Satana?**

Chaputala 7

Chiphunzitso cha Chikonzero cha Mulungu

Gawo 1
Chivumbulutso: Baibulo (Bibliology)

Baibulo linalembedwa ngati mbali imodzi yakudziulula kwa Mulungu kwa mitindu ya anthu. Iye anaziulira yekhanso kupyolera mnzomwe analenga (Aroma 1:20) mawu oti chivumbulutso akutanthauza kuti kuchotsa chovindikira kuti chomwe chinali chobisika chidziwike ndi kuonekera. Mulungu wadziulura yekha komanso kudzionetsera kudzera mu mawu ake olembedwa. Mulungu anadziwonetsera yakha kwa anthu osiyanasiyana mumbiri ya dziko ndipo anawapangitsa iwo kuti alembe za zomwe iye anazivumbulutsira kwa iwo za iye. Ichi chimatchulidwa kuti "kuwuzira."

Pakuti Mulungu anawongolera ndi kuyanganira chivumbulutso chake ndi mzimuwoyera, chinalembedwa popanda kulakwitsa mzolembedwa zoyambilira. Choncho baibulo ngati mawu a Mulungu lili ndi ulamulilo, ndipo potero liri lotitsogolera mmoyo wathu wonse wauzimu.

Kuchokera 1450-400 B.C. Mulungu anatsogolera alembi ambiri polemba mabuku osiyanasiyana okwana 39, amene anaphatikizidwa nkutchedwa chipangano chakale. Pakati pazaka za 46-96 A.D. anatsogoleranso alembi ena ochuluka polemba mabukhu ena 27 omwe amatchulidwa kuti chipangano chatsopano. Mabukuwa akaphatiktzidwa pamodzi amatchulidwa kuti kanoni lomwe ndi lamulo la ekelezia wa malembo oyera. Ophunzira a baibulo akuyenera kudziwa kuti chifukwa choti Mulungu anauzira alembi osiyanasiyana kuti adziwonetsele yekha kwa anthu ndi cholinga choti anthu akhale ndi ulamuliro wolembedwa, mabuku onsewa amene anasonkhanitsidwa kukhala muyeso wa chikhalidwe ndi machitidwe, chinali chokhumba chake.

Zoyenera podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Mutu 7, Gawo 1

1. **Werengani Aroma 1:20. Kodi chilengedwe chimationetsera chiyani za Mulungu?**
2. **Kodi "Bvumbulutso" ndi chiyani?**
3. **Kodi "Kuuzira" ndi chiyani?**
4. **Monga mawu a Mulungu, kodi Baibulo ndi chiyani?**
5. **Kodi chotisogolera pa moyo wathu wa uzimu ndi chani?**
6. **Kodi kuphatikiza kwa chipangano chakale ndi chatsopano kumatchedwa chiyani?**
7. **Werengani Yohane 17:17. Kodi Mawu a Mulungu ndi chiyani?**
9. **Werengani Masalimo 119, ndipo lingalirani, nkhani ya Mawu a Mulungu.**

Gawo 2
Vuto: Tchimo (Harmartiology)

A. Chiyambi

Ntchimo limatanthauza kuphwanya chikhalidwe chimene chinaikidwa ndi Umulungu. Mawu a Mulungu amaneneratu poyera kuti pamayenera kukhala mulingo kuti ntchimo lichitike choncho pakanati palibe mulingu sipakanakhala tchimo (Aroma 4:15; 5:13). Mawu awiri akuluakulu achiyankhulo chachi Heberi komanso chachigiriki otanthauza tchimo (chata komanso hamartia) amatanthauza "kuphonya." Zili ngati kuponya muvi koma otsabaya pakati pomwe munthu amafuna. Ngati munthu sabaya pakati. Ngati munthu waphonya kubaya pakatikati ngakhale anayesera kuyandikirapo, ndiye kuti mwaphonya basi.

B. Pali Mitundu itatu Yosiyanasiyana ya machimo Yomwe Imapezeka Mmawu A Mulungu

1. Ntchimo Lobadwa Nalo

Pobadwa munthu aliyense amakhala okhudzidwa komanso ochimwa chifukwa cha tchimo loyambilira la adamu. Mawu oti "kuyamwira" amatanthauza kuti tchimo linachokera kwa adamu nkulowelera kwa ana ake (tonsefe) kamba ka tchimo lake loyamba. Aroma 5:12 amati , ***"chifukwa cha munthu mmodzi (Adamu) tchimo linaza dziko ndipo imfa inadusira ku tchimo kotero imfa inafara kwa anthu onse.***" Chifukwa onse anachomwa izi zinafotokozeledwa mu Aroma 5:18-19, amati "c***honcho kuchokera mu kulakwa kwa munthu mmodzi (malemba amati Adamu adachimwa) kunabweretsa kudedwa kwa mtundu wa anthu onse, ngakhale ntchito yoyera ya munthu mmodzi inabweretsa moyokwa anthu onse pakuti kusakhulupirika kwa munthu mmodzi kunapagitsa ambiri kuti akhale ochimwa, ngakhalenso kukhulupika kwa munthu mmodzi kuzapangitsa kuti ambiri akhale oyera"*** tchimo la adamu linangitsa kuti munthu wina aliyese akhale ochimwa.

Nzofunika kumvetsa kuti tchimo linadzera kwa atate a padziko lapansi (Adamu), Yesu sadali ndi tate wadziko lapansi, koma tate wa kumwamba,kotero sadakhudzidwe ndi tchimo la Adamu.

2. Tchimo Lachizolowezi

Kamba ka tchimo lobadwa nalo aliyense amategera chikhalidwe chomwe chimapangitsa kuti munthu azipanga machimo. Kawirikawiri izi zimatchedwa "chikhalidwe cha uchimo" kapenanso kuti "munthu wakale." Ngakhale kuti chotsatira cha kuchimwa kwa Adamu chomwe ndi chiweruzo chinachotsedwa, koma chikhalidwe cha uchimo chimakhalabe mwa munthu kufikira imfa yake yakuthupi.

Mtumwi Paulo analemba za kulinbana kwake ndi tchimo lachizolowezi mu aroma 7:16-18 analemba kuti ***"koma ngati ndichita zinthu zomwe sindifuna kuchita, ndigwizana ndi lamulo, ndivomeleza kuti ndilabwino. Ndiye pano, sindili amene ali kuzichita, koma tchimo lomwe lili mwa ine. Pakuti ndidziwa kuti palibe chabwino pa ine, kunena kuti munthupi, pakuti khumbo lili mwa ine. Koma kuchita zabwino ndiko sikuli mwa ine."*** Pa ndime imeneyi tikhoza kumalidzitsa kuti Paulo adangonjako polimbana ndi tchimo lachizolowezi. Akutiuza kuti iyi ndi nkhondo ya Mzimu Woyera (Agalatiya 5:16-17) ndiye okhulupilira wayenera kufunafuna kuti asiye ***zitchito zake zoyipa zakale*** (Aifeso 4:20-22).

Apano ziwani kuti Yesu, potsakhala ndi tchimo lobadwa nalo, adalibenso tchimo lachizolowezi.

3. Tchimo la Munthu Mwini

Awa ndi machitidwe amene amaphwanya malamulo a Mulungu. Ngakhale sitili pansi pa miyambo ya malamulo a Mose, Makhalidwe abwino amene amaphunzitsidwamo amagwilabe ntchito masiku ano. Paulo analemba ku 1 Timoteyo 1:8-10, ***koma tidziwa kuti lamulo ndi labwino ngati wina aligwiritsa ntchito bwino, kudzindikila kuti lamulo sadapangire munthu osachimwa koma onse omwe salitsata ndinso osokoneza, amene Sali a Mulungu komanso ochimwa, omwe Sali oyera ndinso otsalemekeza zinthu zopatulika, omwe amapha abambo ndi amai awo akupha ndi opanda makhalidwe abwino ndinso osilirana akazi kapena amuna okhaokha ndi ogwira anthu azawo mokakamiza ndi aboza zomwe zili kusowa nkhalidwe labwino, kusayera mtima, chigololo, kupembedza mafano, kuombeza, zidani, kaduka, nkwiyo osatha, mikangano, kuledzera, kutentha, ndewu ndi zinthu zina ngati zatchulidwazi zimene ndikuchenjezeranitu monga m'mene ine ndikuchenjezeraanitu kuti onse akuchita izi sazalowa mu ufumu wa kumwamba."***

C. Pali Magulu Atatu Osiyanasiyana a Machismo a Munthu

1. Machimo a M'malingaliro

Mtundu woyamba wa machimo a munthu umagwirizana ndi momwe munthu amaganizira. Yesu akutiuza ku Mateyu 5:28 kuti ***"koma ndinena kwa inu, kuti yense wakuyang'ana mkazi kunkhumba, pamenepo watha kuchita naye chigololo mumtima mwake."*** Mu mtima ndinso mmaganizo anthu

machismo agathe kuyamba. Ndimachimo chifukwa simaganizo achiyero komanso ife anthu timalamulilidwa kuti tikhale oyera mtima, *muzikhala oyera mtima, pakuti ine ndine oyera mtima* (1 Petro 1:16) lamulo la chikhumi pa malamulo a Mulungu, limaletsa tchimo lakulingalila ndi kukhumba zinthu za mwini (Eksodo 20:17) machimo akuganiza, monga machimo enanso a munthu, amaphwanya lamulo lachikondi. Mwa chitsanzo, tchimo lakuganiza lakuzikonda lomwe limapezeka ku Yakobo 2:8-9 lomwe limati ***"ngati ukwanilitsa lamulo lolemekezeka, monga malemba amanenera, konda nzako monga momwe umadzikondera ukatero uchita choyenera.*** Nthawi zambiri machimo a mmalingaliro amaonekera pamene munthu awachita.

2. **Machimo a Mmayankhulidwe**
   Gulu lachiwili la machimo limachokela ku mayankhulidwe a munthu. Buku la Yakobo lili ndi gawo lalikulu pa nkhani ya zoipa za nkuyakhula (Yakobo 3:1-10) machimo akuyakhula ananenedwa moveka pa lamulo lachisanu ndi chinayi pa malamulo khumi a Mulungu, lomwe limati ***usaikire umboni wonama kwa mzako*** (Eksodo 20:16) Satana (kutanthauza kuti opandukila), amene ali mdyerekezi (kutanthauza kuti wakaduka) ndiye tate woononga anthu ena kudutsira mu mawu. Chizindikilo chachikulu cha tchimo lakuyankhula ndichakuti, zomwe zayankhulidwa sizimalankhulidwa mwa chikondi cha pa Mulungu kapena pa anthu ena.

3. **Machimo Owonetsera Poyera**
   Gulu lachitatu komanso lomaliza la machimo limachokera ku kuzimene munthu amachita. Izi ndi zinthu kapena ntchito zimene munthu amapanga. Zitsanzo zabwino za gulu ili lamachimo, zimapezeka pa lamulo la chisanu ndi mchimodzi, chisanu ndi ziwiri komaso chisanu ndi zitatu mumalamulo nkhumi a Mulungu:
   1) "usamphe"
   2) "usachite chigololo"
   3) "komanso usabe"

   Yakobo 4:17 amati, ***"munthu amene adziwa choonadi koma osamachichita wachita tchimo."***

   Nchofunikira kudziwanso kuti machimo ena amatha kukhala ophatikiza magulu onse atatu tatchulawa. Yesu ananena poyera kuti kupha kutheka kukwaniritsidwa mu maganizo, pakuyankhura komanso pakuchita ntchito yakunchotsera nzako moyo (Mateyu 5:21-23).

   Yesu sanachitepo gulu lililonse la machismo a munthu.

Zoyena podziyesa aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Mutu 7, Gawo 2

1. **Werengani Aroma 4:15, Aroma 5:13. Kodi uchimo kuti uchitike, pamakhala chiyani?**

2. **Werengani Aroma 5:12, 18:19. Tchulani zotsatira za kuchimwa kwa Adamu ndipo ndi chifukwa chiyani?**

3. **Werengani Aroma 7:16-18. Kodi chikhalidwe cha uchimo chimakhala kuti?**

4. **Werenngani Agalatiya 5:19-21. Machimo a munthu ndi chiyani?**

5. **Werengani Mateyu 5:28. Tchulani mtundu wa tchimo womwe wafotokozedwa.**

6. **Werengani Yakobo 3:1-10. Tchulani mtundu wa uchimo womwe wapezeka mu nkhaniyi?**

7. **Werengani Eksodo 20:13-15. Kodi ma vesi awa akunena mitundu iti ya uchimo.**

8. **Machimo omwe alembedwa mu Agalatiya 5:19-21 aperekedwa. Longosolani bwino machimowa powona ngati ali a mmaganizo, olankhula kapena ochita. Ena akhoza kukhala ophatikiza magulu angapo.**
   a. Dama
   b. Chodetsa
   c. Kukhumba zonyasa
   d. Kupembedza mafano
   e. Nyanga
   f. Madano
   g. Njiru
   h. Zotetana
   i. Ndewu
   j. Zopsa mtima
   k. Magawano
   l. Kuledzera
   m. Mcezo
   n. Kaduka
   o. Mipatuko

Gawo 3
Yankho: Chipulumutso (Soteriology)

A. Malonje

Podziwa kuti uchimo ndi vuto la anthu kupatula Yesu Khristu, anthu onse akufunika kuti apulumutsidwe kuchokera ku zotsatira zake. Mulungu, mu ukulu wake, ndi mwamphamvu zonse, anapangiratu ndondomeko zoti munthu apulumutsiridwirepo. Ndipo ndondomekoyi dipo lake linali imfa ya Yesu Khristu. Yesu anakwaniritsa choonadi ndi chilungamo cha Atate, popereka dipo lomwe munthu sangakwanitse. Ili linali dipo latchimo. Munthu akuyitanidwa kulandira nsembe ya Yesu kudzera mu Chikhulupiliro (2 Akorinto 8:9).

B. Uthenga Wabwino

Mawu oti "Uthenga," akutanthauza "Uthenga Wabwino." Uthenga wabwinowu ndi wakuti, Chipulumutso chilipo kudzera mu chikhulupiliro mwa Yesu yekha. Pa Machitidwe 16:30, silikari wa chiroma anafunsa Paulo, "Kodi ndichitenji kuti ndipulumuke?" Paulo anayankha "Khulupilirani mwa Yesu Khristu, ndipo mudzapulumutsidwa (Machitidwe 16:31). Chikhulupiliro, mwa Yesu Khristu, chakambidwa momveka bwino kuti ndiyo njira yokhayo yofunika pa chipulumutso (Yohane 3:16, 18, 36). Palibenso dzina lina padziko, lomwe tingapulumuke nalo, koma la Yesu Khristu lokha (Machitidwe 4:12).

Cholinga cha Mulungu ndi chakuti anthu apulumutsidwe (1 Timoteo 2:4; 2 Petro 3:9), ndipo Yesu Khristu, analipira dipo pa machimo a dziko lonse lapansi (1 Yohane 2:2), kuti afike anthu onse chifupi ndi Mulungu (Yohane 12:32). Mzimu woyera, amatsutsa dziko lonse pokhudza vuto la uchimo, ndipo amaulula kuti Yesu Khristu ndiye yankho (Yaohane 16:7-15).

Choonadi chenicheni, ndi choti, munthu ayenera kuvomereza za Yesu Khristu ponena kuti, Yesu anali Mulungu yemwe anakhala pa dziko monga munthu (Yohane 1:1, 14), anafa pofuna kupereka dipo pa uchimo, anaikidwa m'manda, (kusonyeza kuti iye anafadi) ndipo kuti, anauka m'manda, tsiku lachitatu (1 Akorinto 15:3-5).

C. Chisomo

Chisomo chikutanthauza kuti, tapatsidwa chinthu china chomwe sitinayenera kukhala nacho. Ngati tinalandira zinazake, awa amakhala "malipiro" omwe talandira, malinga ndi ntchito zawo**.** Chisomo chomwe tachilandira mu chipulumutso, ndi mphatso yochokera kwa Mulungu. Malemba akunena kuti ***"Popeza kuchokera mu chisomo, tinapulumutsidwa mwa chikhulupiliro, osati mwa inu nokha, koma monga mphatso yochokera kwa Mulungu, osati monga zotsatira za ntchito, kuti wina anganyadire"*** (Aefenso 2:8-9). Chisomo cha Mulungu chinapereka mphatso ya chipulumutso yomwe ife tiyenera kuilandira mwa chikhulupiliro. Uthenga wabwino umalongosoledwa kuti, ndiwo chisomo cha Mulungu (Machitidwe 20:24).

Yesu Khristu mwini, anali chitsanzo cha chisomo pa anthu (Yohane 1:14-17).

D. Chikhulupiliro

Chikhulupiliro ndicho kukhulupilira kapena kudalira. Ndipo nkhani yagonera pa iye amene timukhulupilirayo osati munthu okhulupilirayo. Chikhulupiliro chimakhudzana ndi kulandira Yesu Khristu. Chikhulupiliro si ntchito.

Monga anthu, timakhumba kulandira chipulumutso chathu, koma anthu ochuruka amalakwitsa pokhulupilira kuti ayenera kuchita ntchito kuti apulumutsidwe, mmalo mongolandira mphatso yochokera kwa Mulungu. Ndi zoona kuti Mulungu analenga ntchito ***"zabwino mwa ife"*** (Aefenso 2:10), koma ife tiyenera kugwira ntchito yabwino monga Zotsatira za chipulumutso osati kuti tilandire chipulumutso chifukwa cha izo.

Tsiku lina mu utumiki wa Khristu, Iye anali kuphunzitsa za moyo wosatha kuti inali mphatso yomwe iye anakhoza kuipereka (Yohane 6:26-27) Anthuwo anamfusa Yesu ***"Tichitenji kuti tigwire ntchito, ntchito za Mulungu?"*** (Yohane 6:28). Ndipo Yesu anati. ***Iyi ndi ntchito ya Mulungu kuti mukhulupilire "Iye amene anadituma"*** (Yohane 6:29) Apa Yesu amatanthauza kuti, ngati mukhulupilira, muyenera kugwira ntchito kuti mupulumutsidwe, ndipo adatchula chikhulupiliro chotero, ntchito. Kukadakhala kuti chikhulupiliro chathu ndi ntchito, ndiye ntchitoyo ikadaposedwa ndi ntchito ya Mulungu ya Chipulumutso, ndipo ntchito yathuyo ikadakhala yopanda phindu nkomwe.

Mulungu amapereka kwa yense, mphamvu yokhala ndi chikhulupiliro, mphamvu yopanga chisankho. Iyi ndi mbali yaikulu yotanthauza ***"Kulengedwa mu chifanizo ca Mulungu"*** (Genesis 1:26-27). Ngakhale munthu anapatsidwa kuthekera kwenikweni, kuti asankhe, sizikusonyeza kuti iye adzasankha bwino nthawi zonse. Kuthekera kopanga chisankho, kumapangitsa munthu kukhala mwini wa chisankhocho. Popeza munthu wina aliyense ali ndi ufulu wosankha, onse omwe sanasankhe Khristu, agalukira iye (Mateyu 12:30; Yohane

3:18). Koma kusankha Khristu Kumabweretsa moyo wosatha kumwamba. Pomwe kusankha motsutsana ndi Khristu ndiko kuziitanira chilango ndi imfa yosatha ku moto (Yohane 3:36).

E. Kulapa

Kulapa kumatanthauza kuti "kusintha maganizo" zimatanthauza kuti mchitidwe wasinthidwa kapena kusiidwa kupita ku mchitidwe wina. Mulungu amafuna yense wakusakhulupilira kuti asinthe nkusata Yesu Khristu kuti asadzaonongeke (2 Petro 3:19; Machitidwe 20:21). Izi zimaphatikiza kuzindikira kuti anthu sangalipire kapena kudzipulumutsa ku machismo awo, koma kuti Yesu analipira ngongole ya machismo awo pakutifera tonse (Luka 24:45-47). Kulapa ndi chiyambi chamoyo watsopano wa chikhristu (Ahebri 6:1).

Okhulupilira amatha kusinthanso maganizo nthawi zina ngati azindikira kuti zomwe amakhulupilira kuti ndi zoona sizli zoona konse (2 Timoteo 2:24-25) kapena chomwe samazindikira kuti ndi tchimo lili tchimo (2 Akorinto 7:9-10). Machimowa (ndi ena onse) ayenera kulapidwa kwa Mulungu (1 Yohane 1:9).

F. Kulungamitsidwa

Kulungamitsidwa kumatanthauza kuti wayesedwa ndipo wapezeka wopanda mulandu kapena wolungama. Munthu pokhala wochimwa, iye Sali olungama komanso sangakhale olungama mpaka m'mene Mulungu amafunira, choncho sangafanane ndi Mulungu komanso kukhala pa ubale wabwino ndi Mulungu (Yesaya 64:6; Aroma 3:20). Ili ndivuto lalikulu ku mtundu wa anthu: Kodi munthu angakhale bwanji olungama kuti akhale pamaso pa Mulungu? Yankho likupezeka mu chiphunzitsochi.

Gawo lofunikira kwambiri likupezeka pa (Aroma 3:19; 4:5) limanena kuti: (1) palibe angakhale olungama chifukwa cha ntchito za lamulo (3:20 cf. Agalatiya 2:16; 3:24); (2) kulungama ndi mphatso ya chisomo chifukwa Khristu analipira ngongole ya machismo athu (kuomboledwa) zimene zinakwaniritsa zofuna za Mulungu, muchiyero ndinso muchilungamo chake (3:24); (3) kulungamitsidwa ndi kukhala ndi chikhulupiliro mwa Yesu (3:26). Yense okhulupilira Yesu Khristu amapatsidwa chiyero ndipo amasanduka munthu oyera mtima.

Kulungamitsidwaku mwa chisomo kudzera mu chikhulupiliro mwa Yesu zimatikhalitsa pa mtendere ndi Mulungu (Aroma 5:1), kumatipulumutsanso ku mkwiyo wake umene umabwera chifukwa cha kulungama komanso chilungamo chake cha Mulungu (Aroma 5:9). Kumatimasulanso ku chilango chimene tiyenera kulandira chifukwa cha chikhalidwe cha uchimo (Aroma 6:7) natipatsa cholowa ndi Khristu (Tito 3:4- 7).

G. Kuyeretsedwe

Kuyeretsedwe kamatanthauza kuti kupatulidwa kukhala oyera. Chiyero kumaonedwa poona kulungama ndinso chilungamo cha Mulungu. Pamene munthu alungamitsidwa mu chisomo kudzera muchikhulupiliro cha Yesu Khristu, munthuyo amakhalanso kuti wapatulidwa ndi Khristu (Machitidwe 26:18; Aheberi 2:11) kupyolera mu nsembe yake imene anayipeleka kamodzi (Aheberi 10:10-14; 13:12) komanso ndi Mzimu Woyera (2 Atesalonika 2:13; 1 Petro 1:2). pamene takhala okhulupilira tiyenera kugawana chiyerochi ndi anthu ena (Ahebri 12:14).

kuyeretsedwa sikukutanthauza kuti moyo wa okhulupilira sukhala ndi tchimo lililonse ayi. Mpingo waku Akorino udalakwitsa mu gawo ambiri a moyo, komabe adapatulidwa mu Khristu ndipo amatchedwa "anthu oyera mtima" (1 Akorinto 1:2, 30; 6:9-12).

Okhulupilira ayenera kutenga Yesu Khristu ngati chitsanzo chabwino cha chiyero m'moyo wawo (1 Atesalonika 4:3, 4, 7; Aefeso 5:25-26; 1 Petro 3:15). Izi zimaphatikira mu njira ya kayeretsedwe imene imatsatira kayeretsedwe kamene kamachitika pamene munthu wangopulumutsidwa kumene (Aroma 6:9; 1 Atesalonika 5:23). Njira iyi imakwaniritsidwa pokhulupilira mu chilungamo chopezekera mu mau a Mulungu (Yohane 17:17-19) komanso kudzipereka kwa thunthu kwa Mulungu kuti uyeretsedwe kuti ukhale ku phindu kuntchito iliyonse yabwino (2 Timoteo 2:21). Zopereka za okhulupilira zimakhala mwa Khristu zopatulika kudzera mwa Mzimu Woyera (Aroma 115:15-16). Amene sachita izi amachitila mwano chisomo ndipo adzalandira chidzuzulo chachikulu kuchokera kwa Mulungu (Ahebri 10:29).

H. Kukhululuka

Kukhululuka kumatanthauza "kuzitaya kutali zinthu zodana ndi wina." Izi zikuchokera ku mau achi Greek oti "APHLEMI" amene amamasulidwa kuti "kuchoka" (Mateyu 4:20, 22; 5:24). Monga munthu amachoka malo amodzi kunka malo ena, chonchonso machimo amasiidwa m'mbuyo sakhalanso chipsinjo choti nkunyamula (Ahebri 12:2). Yesu asadapachikidwe pa mtanda, machimo adalipo koma "ankangophimbidwa" kutanthauza kuti ankakhalapobe koma kuti chiweluzo chake chinagwiridwa kapena kusungidwa (Masalmo 32:1 cf. Aroma 4:7). Imfa ya Yesu pamtanda inatengera machimo kutali nafe. Machimo athu anakhululukidwa (Mateyu 26:27-28). Kukhululuka linali gawo lofunika kwambiri pa uthenga wa yohane m'batizi (Luka 3:3-4) ndinso Yesu Khristu (Luka 4:18-19; Machitidwe 5:31). Kukhululuka kukhoza kukhala ku zinthu zimene tili nazo ngongole (Mateyu 6:12-15), machimo (Mateyu 9:2-6) kapena khumbo la mtima (Machitidwe 8:22).

Kukhulukidwa kwa machimo ndi gawo lofunika kwambiri mu njira yachipulumutso (Luka 1:17). Nsembe ya Yesu Khristu, yomwe idalipira ngongole yathu yamachimo yomwe tidapalamura kwa Mulungu inali gawo loyamba la chikhulupiliro (Aefeso 1:7; Akolose 1:13-14; Ahebri 9:22). Pamene munthu akhulupilira Yesu Khristu amakhululukidwa machimo ake (Machitidwe 110:43; 26:18). Popeza Yesu anatifera pamtanda kuti machimo athu akhulukidwe, sipazakhalanso nsembe ina yomwe izatipulumutse kumachimo (Ahebri 10:17-18).

Pamene chikhululuko ndi chisomo chomwe chimatitayanitsa ndi machismo, Mulungu anachitanso chinthu china chozizwisa pa moyo wathu. Tonse timadziwa pamene tasiya ka chovala pa mbuyo, timatha kubwerera nthawi ina kukatenga. Mulungu sangosiya machimo athu kutali ayi koma amawachoseratu. Tinauzidwa kuti, ***"ndipo inu pakukhala akufa m'zolakwitsa ndikusadulidwa kwa kwa thupi lanu, anakupatsani moyo pamodzi ndi iye m'mene anatikhulukira ife zolakwa zonse; adatha kutifafanizira cha pa ifecho cholembedwa nzoikikazo, cchimene chinali chotsusana nafe; ndipo anachichoesera pakatipo, ndikuchikhomera ichi pa mtanda"*** (Akolose 2:13-14). Chifukwa chakuti machimo athu samangosiidwa pambali pokha chabe koma kuti amachokeratu, zimenezi ziyenera kutipangitsa kuti tikhalenso anthu osisimuka pamaso pa Mulungu (Machitidwe 3:19).

Okhulupilira ayenera kudzakhala ngati Mulungu (Aefeso 5:1) ndinso Yesu Khristu (1 Akorinto 11:1), zimene zikungotiphunzitsa zakufunika ko khululuka (Mateyu 18:21-22). Nzofunikira kwambiri kuti akhristu azikhala anthu okhululuka pakuti kukhululukira ena kumapangitsa kuti machimo ako akhululukidwenso komanso ndi zimene ambuye watituma kuchita (Luka 24:46- 47; Machitidwe 10:43; 13:38). Tayenera kukhala mu zomwe timaphunzisa.

Pamene okhulupilira wachimwa, nzoffunikira kuti alape machismo kwa Mulungu kuti akhulukidwe ndinso kuyeretsedwa (1 Yohane 1:6-10) kuti apitilire kukula mu uzimu. Yesu anatifera pa mtanda kuti machimo athu akhululukidwe, kotero tili kale okhululukidwa. Pamene okhulupilira walapa machismo akwe, akuzindikira kuti ngongole yake ya machismo idaperekedwa kale.

I. Tchimo Losakhululukidwa (Kunyoza Mzimu Woyera)

Pali tchimo limodzi limene silikhulululidwa: kunyoza Mzimu Woyera (mateyo 12:31-32). Kunyoza Mulungu ndiko kumunena zomwe iye saali. Pamene munthu apandukira Mulungu nanena zimene Mulunguyo sali, ndiye kuti wanyoza Mulungu. Mzimu oyera, Mzimu wa chilungamo (Yohane 14:17) umawonetsera poyera kuti Yesu Khristu ndiye mesaya, (Yohane 14:6; 16:13). Pamene munthu akana kuti Yesu si mesaya kapena mpulumutsi, amakhala akukana kuti kapena kunena kuti Mulungu akunama za Yesu (1 Yohane 5:10). Ndikhulupilira kuti mwazindikira tsopano kuti munthu ali ndi mwayi ovomera Yesu ngati mesiya akanali ndi moyo padziko lapansi pano. Titati tione mfundo zonse, kunyoza Mzimu Woyera kutanthauza kutchura Mzimu Woyera ngati wabodza pa za Yesu Khristu mpaka imfa yako. Sizitanthauza pa za mau aphuzo okhaokha kwa Mulungu (cf. Petulo anamkana Yesu Khristu mu Mateyu 26:74) koma ndi tchimo losakhulupilira lomwe limakhalapo mpaka imfa ya munthu. Tchimoli ndikukanisitsa ntchito za Yesu Khristu ngati mpulumutsi zomwe zimakuika pa chiopsezo chachikulu chopita ku gehena**.**

Zoyenera kuchita aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Mutu 7, Gawo 3

1. **Werengani Yohane 3:16, 18, 36. Kodi chofunika ndi chiyani pa chipulumutso?**
2. **Werengani Yohane 1:1, 14, 1 Akorinto 15:3-5. Munthu akhulupilire chiyani, za Yesu Khristu?**
3. **Werengani 1 Timoteyo 2:4, 2 Petro 3:9. Zokhumba za Mulungu pa chipulumutso cha munthu ndi zotani?**
4. **Werengani Aefenso 2:8-9. Munthu adzapulumutsidwa bwaji?**
5. **Chikhulupiliro ndi chiyani ndipo chagonera pati kapena pachani?**
6. **Werengani 2 Timoteo 2:24-25. Kodi zofunika kusintha maganizo a munthu ndi zotani?**
7. **Werengani Aroma 3:20, Agalatiya 2:16, Agalatiya 3:24. Kodi chimatilungamitsa Ife pamaso pa Malungu ndi Chiyani? Nanga chomwe sichimatilungamitsa Ife ndi chiyani?**
8. **Werengani 2 Atesalonika 2:13, 1 Petro 1:2. Kodi amalungamitsa okhulupilira mwa Yesu Khristu ndi ndani?**

9. **Werengani Aefenso 1:7, Akolose 1:13-14. Okhulupilira amakhululukidwa chifukwa chiyani?**

10. **Werengani Mateyu 12:31-32, Yohane 14:17, Yohane 16:13, 1 Yohane 5:10. Kodi kunyozetsa Mzimu woyera ndi chiyani?**

Gawo 4
Chitetezo: Malonjezo a Mulungu

A. Chiyambi

Pamene munthu wapulumusidwa chifukwa cha chikhulupililo mwa Yesu Khristu mafunso ambiri amabwera monga, kodi tingataye chipulumutso chathu? nanga ngati wachimwa utapulumutsidwa, ndikoyenera kuti tipulumutsidwenso? Kodi timakhala bwanji mmoyo wachikhristu- podalira chikondi cha Mulungu kapena mwamantha kuopa kutaya chipulumunso chanthu? Kodi tingadziwe bwaji kuti tili ndi moyo wosatha (1 Yohane 5:13)? Mbali iyi yaphudzilo iwonetsa zoona zokhuza chipulumunso chathu ncholinga choti okhulupilira ayankhe mafunsowa.

B. Chidziwitso pa zinthu za mtsogolo ndi kukhazikitsiratu zinthu

Chidziwitso cha zinthu zamtsogolo zitanthauza kuti "kudziwiratu chinthu chitsanachitike". Yesu anadziwikiratu dziko litsanalengedwe (1 Petro 1:20) mawu oti "Kukhazikitsiratu" anachokera ku Greek "prooridzo omwe akutathauza "kulembeleraru" monga mwakukhazikitsa malire.

Ndizodziwikiratu bwino kuchokera mmawu a Mulungu kuti chidziwitso chake ndicholingana ndi kukhadzikitsiratu kapena kusankhiratu kale kwa zinthu zonse (Aroma 8:29-30; 1 Petro 1:1-2) Nzeru za Mulungu zotsatha zinapangitsa otsati kudziwa kokha ganizo lili lonse loti lizapangidwe ndi zinthu zoti zizachitike, koma anadziwa zonse zomwe zingachitike komanso momwe zingachitikire. Ukulu wa Mulungu umaoneka pomwe iye amapanga ndondomeko mwa iye yekha yomwe anapereka kwa anthu ake komanso angelo ake mphamvu zotsankha koma pamapeto pake pa zonse dongosolo lake limakwanilitsidwa.

Mauneneri kapena ulosi wa m'baibulo unapangidwa kuti uwonetsere nzeru zakuya za Mulungu kapudziwiratu zomwe zizachitike mtogolo (2 Petro3:17) tingathe kudziwiratu bwino mwa zinthu zina zomwe zidzachitike mtsogolo kotero tingathe kutsakha kukhala mbali ya Mulungu kapena ya Satana.

C. Mapangano

Mfundo ya chisanu ndi chitatu ya kutanthauzira mawu inakambako za malonjezano asanu ndi anayi amene Mulungu anapangana ndi munthu. Ena ayiwo amatengera kuti munthu wamvera kapena ayi. Ena mwa mapanganowa satengeranso kuti munthu akumvera kapena ayi koma amatengera kukhulupilika kwa Mulungu. Mapangano amenewa ali ndi malonjezano a Mulungu amene amamupangitsa okhulupilira kukhala wotetezeka pano komanso ku muyaya. Ophunzira awonenso bwino uthenga umene uli pa mapangano ndikulingalira za chitetezo chimene tilinacho kolingana ndi malonjezano a Mulungu.

D. Chitetezo Chosatha

Chitetezo chosatha chitanthauza chipulumutso chomwe sichingatayike. Tipitiliza kufufuza mfundo imeneyi pogwiritsa ntchito malamulo omwe taphunzila. Tiyeni tikumbukire kufunika kwa kuganiza mofatsa pamene tikukambirana za mutuwu. Ngati tipeza mmawu a Mulungu uthenga wa kwa tonse wotiuza kuti sitingataye chipulumutso chanthu chosatha ndiye tiyenera kuvomereza izi kuti nzoona, pokhapokha titapeza mawu enanso amene akulankhula zina zosiyanilanako. Ndizomvetsetseka kuti ngati buku loyera linena kuti ichi nchoona tidziwenso kuti ndi baibulo lomwelo limene likhoza kupatulako zinthu zina ku chiganizocho. Mwachitsanzo, malemba amanena kuti, ***"onse anachimwa ndipo apelewera pa ulemelero wa Mulungu"*** (Aroma 3:23) chopatulika chokhancho chomwe chalembedwa ndichoti Yesu Khristu amene timamuyembekezela "***sanachimwepo"*** (1 Petro 2:22). Pali njira ziwiri zoyan'ganira zinthu. Njira yoyamba imatchedwa "Dedactive." apa timayan'gana chinthu chachikulu kaye kenako mkumaona zin'gonozin'gono zomwe zapanga chinthu chachikulucho. Njirayi ndiyabwino chifukwa imapeleka mayankho olondola mosavuta. Mwachitsanzo, "Ngati onse anachimwa kupatula Yesu, ndiye kuti ine ndinachimwa." Njira ina imayamba kuyan'gana zinthu zin'gonozin'gono kenako nkuzamalizira chachikulu chopangidwa ndi zazin'gonozo. Chitsanzo, "chifukwa choti ndinachimwa, ndiye kuti aliyense anachimwa" Kaganizidwe kamtundu otere kamatilondoleranso ku yankho koma zoti Yesu sanachimwepo, zimene ndizoziwikilatu, zimatiwonetsa kuti njirayi ili ndi zofooka zambiri. Zimavuta kwambiri komanso kusochera kumakhalapo pamene gawo limodzi lomwe likupanga nawo chinthu chachikulucho lasiyidwa.

Umboni wathu wokhuzana ndi chietetezo chosatha kwaonetsedwa m'njira zinai:

1. **Kuganiza molingana ndi zinthu mmene zimvekera/kuonekera**
   Tione zitsanzo zitatu izi: choyamba, pakuti muli opulumusidwa ndi chisomo chakuchita mwachikhulupililo, ndipo ichi chosachokera ku ntchito, ndiye kuti chipulumutso sichingatayike kudzera mu ntchito ngati tchimo (Aefeso 2:8-9). Chachiwiri, pakuti kubadwanso mwatsopano kumatipangitsa ife kukhala ana a Mulungu, ndiye kuti kulephera kwathu sikungapangitse kuti Mulungu asakhalenso atate wathu (Yohane 1:12-13; 2 Timoteo 2:13). chitsanzo chomaliza nchakuti, chifukwa chakuti anatipangira

kale zambiri tili adani ake ndikutipulumutsa, panopa sangabwelere mbuyo pokhala kuti tinapulumutsidwa ndikutitaya (Aroma 5:9-10).

2. **Kutengera Pamene Chithu chili**
   Njira iyi pokhuzana ndi chitetezo cha chipulumutso cha okhulupilira chikuchokera pa choonadi choti okhulupilira "ali mwa Yesu ndipo kuti palibenso kutsistidwa kwa onse amene ali mw Yesu" (Aroma 8:10) mwa Yesu chikondi cha Atate (mulunngu) kwa okhulupilila ndichofanana ndi chikondi chake kwa Mwana wake, makamaka pokhala kuti ifenso ndi ana ake (Yohane 1:12-13; Aroma 8:38-39; Agalatia 3:26; Afeso 1:5-8) Ndipo ife tilandira kale chiukitso cha khristu, pakuti tinawuka naye limodzi ndipo sitidzafa (Aefeso 2:6). Chofunika china kudziwa ndichoti mutu sungachonse ziwalo zake za thupi ndi kukhalanso thupi lonse (1 Akonrito12:13). Tonse tizakhalabe gawo la iye.

3. **Kutengera njira yakutetezera**
   Njilayi ikuchokera pa machitidwe a Yesu ku dzanja la manja la Atate komwe ali mtetezi wathu kwa tSatana (1 Yohane 1-2; Chivumbulutso 12:10) iye anali nkhalapakati Pakati pa Mulungu ndi mnthu pomwe anamupezela munthu pangano labwino (Agalatia 3:20; 1 Timoteo 2:5; Ahebri 8:6; 9:15; 12:24) panopa iye amawapembedzera osankhika a Mulungu kuti asungike komanso atetezeke (Aroma 8:31-39) aliyense woyesera kukwatula nkhosa zake ku mkono wake akulimbana ndi mphamvu za Mulungu zosatha ndi Mwana wake (1 Yohane 10:27-29) chomwe mulembi wazindikira nchakuti Ichi ndicho chitetezo kwa iye.

4. **Kutengera ntchito za moyo wauzimu**
   Njirayi ikutengedwa kuchokera pa ubale wa munthu ndi Mzimu Woyera. Mzimu Woyera amatenga mnthu amene sanapulumuke obadwa muthupi la "kambeu kotha kuonongeka" ndipo pamene munthuyu akhulupilira mwa Yesu khristu amamupangitsa kubadwanso ndi "mbewu yomwe singaonongeke." potero ife sitingafenso (1 Akorinto 15:42, 52; 1 Petro 1:22-25; Yohane 11:25-26). Pali mphatso zosiyanasiyana zimene zinapasidwa kwa ife panthawi imene tangopulumusidwa zimene zimakhala zaphumphu komanso zosalapika, kuchokera kwa Mzimu Woyera (Aroma 12:29). Mzimu Woyera umakhala mwa okhulupilira pamene wapulumutsidwa (Aroma 8:9; 1 Yohane 2:27; 2 Akorinto 1:22). Mzimu Woyera umabatiza omwe akukhulupilira mu umodzi wa Yesu Khristu (Aroma 8:9; 1 Yohane 2:27) ndikumuyika chizindikiro kufikira tsiku la chiwombolo (2 Akorinto 1:21-22; Aefeso 1:13; 14:14-30).

E. Kutengedwa kukhala mwana

Yesu Khristu ndi mwana yekhayo wa Mulungu obadwa yekha (Yohane 3:16). Pamene tikhala mu umodzi ndi Yesu Khristu mu kukhulupilira, timaoneka ngati ana osandutsidwa ake a Mulungu. Kutengedwa uku kunalinganizidwa kwa ana onse a Israeli, koma ambiri anakana mpulumutsiyo (Aroma 9:3-4).

Wokhulupilira ali ndi mwayi wokhala pa ubale weniweni ndi Mulungu komanso Mwana wake pozindikira kuti iye ali olowa pamodzi naye Yesuyo (Aroma 8:15-17; Agalatiya 4:4-7). Tsiku lina tonse tizazindikira bwino lomwe madalitso akukhala wakewake (Aroma 8:22-23).

Zoyenera kuchita aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Mutu 7, Gawo 4

1. **Werengani 1 Yohane 5:13. Munthu angadziwiwiretu kuti wapulumutsidwa?**

2. **Werengani Aroma 8:29-30, 1 Petro 1:1-2. Kodi mulungu amagwiritsa ntchito chiyani posanja zochitika?**

3. **Werengani Yohane 10:27-29. Kodi Yesu analonjeza chiyani ku nkhosa zake?**

4. **Werengani Aefenso 2:8-9, Aroma 11:29. Popeza chipulumutso ndi mphatso, kodi Mulungu angailande?**

5. **Werengani Yohane 1:12-13, 2 Timoteo 3:13. Okhulupilira, akayamba chikaiko, kodi amachoka kukhala mwana wa Mulungu?**

6. **Werengani Aroma 5:9-10, Luka 6:31-36. Kodi Mulungu anatipulumutsa, M'mene tinali adani ake? Kodi chimationetsera Chikondi cha Mulungu ndi chiyani?**

7. **Kodi ndi za nzeru kunena kuti popeza Mulungu anatipulumutsa kutichotsa ku udani kukhala ana ake, angadzatiponyenso pansi?**

8. **Werengani Aroma 8:1. Polingalira momwe tiri mwa Khristu, ndi chiyani chomwe kulibe?**

9. **Werengani Aroma 8:35-39, Chingatilepheretse ife Chikondi cha Mulungu ndi chiyani?**

10. **Werengani 1 Petro 1:22-35. Popeza tabadwa kuchokera ku mbewu yosafeka mwa Mzimu Woyera, Kodi tidzafanso kawiri?**

11. **Werengani Aroma 8:15-17. Ubale wa munthu ndi Mulungu ndi wotani?**

Gawo 5
Mtsogolomo: Uneneri (Chiphunzitso cha zinthu za mtsogolo)

A. Chiyambi

Mulungu mwa chisomo chake waikiratu dongosolo ku mibadwo mibadwo. Akutidziwitsa za nyengo zosaiwalika zomwe zizakhalepo. M'nyengo zina akutambasura zambiri, ndipo nthawi zina akupereka zochepa. Tikhoza kukhala ndi chikhulupiliro podziwa kuti Mulungu wathu amaziwiratu za mawa.

Uneneri ndilo phunziro la mphamvu la mau a Mulungu. Ma machaputala 1189 omwe akupezeka mbaibulo, 271 akukamba za uneneri. Machaputalawa ndi pafupifupi theka la theka la baibulo. Aliponso mavesi oonjezera ambirimbiri m'baibulo omwe akukamba za uneneri kotero kufufuza za uneneri nkofunika.

Pamene tikufufuza za uneneri tikuyenera kuziwa za zochitika zomwe sizidachitikepo. Izi zitithandidzira kukhala ndi chithuzithuzi momwe tingafufuzire za uneneri. Kumbukirani mu mfundo 15 ya kafufuzidwe kathu mu"malamuro ofunikirazo kwambiri potanthauzira" mu chaputala kapena mutu wa chinai kuti ma uneneri ena anakwanirisidwa ndipo ena sanakwanirisidwe.

M'kufufuza kwathu tikuyenera kudziwa mau osiyanasiyana omwe amagwirisidwa ntchito pokamba za mtsogolo.

B. Nthawi za mmibado ya m'mbuyo

Uneneri umalumikizana bwino ndi nkhani ya "nthawi za mibado yakale". Ndikofunika kuti ophunzira atabwereza mfundo ya khumi ndi chitatu mu malamuro ofunikira kwambiri potanthauzira, imene imakhuzana kwambiri ndi nthawi za mibado ya mmbuyo.

Nthawi zimenezi ndi nyengo zokumbukilika zomwe Mulungu anapereka ulamuliro osiyanasiyana kwa anthu ake. Pali kusintha kwa unsembe komanso chilamuro kumene kwaonetsera kusintha kwa machitidwe a zinthu mu nthawi yoikika (Ahebri 7:12).

Zaka za anthu achikunja zimene zinayamba mu nthawi ya kuchimwa kwa Adamu kufikira kumapeto kwa ulendo wa ana a Israeli kuchokera mdziko la Egypt inatha. zaka za ana a Israeli zinayambira pa ulendo wawo (Pakupasidwa chilamulo) kufikira tsiku la Pentekoste. Zidamalizika kupatulika ka nthawi ka zaka zisanu nziwiri nkonenedwa kuti "mlili" kapena "masabata makumi asanu ndi awiri a Danieli" (Danieli 9:24-27).

Tsopano tili mzaka za mpingo zomwe zidayamba pa tsiku la Pentekoste ndipo zipitilira mpaka pa tsiku la mkwatulo wa mpingowu.

Kutsogoloku kuzabwera zaka zimene Yesu Khristu adzabwere kachiwiri kuzakhazikitsa ulamuliro wake kwa zaka chikwi zomwe zizathe ndi kuukira komaliza kwa Satana.

C. Mkwatulo

Mawu oti mkwatulo amachokera pa mau a chi latini oti "RAPERE" omwe adagwiritsidwa ntchito pomasulira mau a chi Greek oti "HARPADZO" opezeka pa 1 Atesalonika 4:17, m'baibulo lomasulilidwa m'chilatini. M'chingerezi amatanthauza kutengedwa.

Pa mkwatulo, ambuye adzaukitsa okhulupilira omwe adamwalira limodzinso ndi okhulupilira omwe adzakhale ndi moyo dipo adzawatengera mlengalenga momwe adzakumane nawo (1 Atesalonika 4:14-17). Izi zizachitika mkaphindi (1 Akorinto 15:51-54).

Mkwatulo udzathetsa zaka za mpingo ndipo udzayambitsa nyengo ya mliri kapena chisautso.

D. Chisautso

Mau oti chisautso amachokera mu mau a chi Greek "THLIPSIS" omwe amatanthauza kuti "kufinyika," mwachitsanzo munthu akaponda nyumwa ndi mapazi. Ndi nthwi yowawitsa zedi imene dziko lapansi silidakhalepo mu nthawi ngati imeneyi. Chidule cha zomwe zizachitike pa nthawi ya chisautso zikupezeka pa Chivumbulutso 1:6-19.

Chisautso chizakhalapo kwa zaka zisanu ndi ziwiri zomwe zimatchulidwa "sabata ya makumi asanu ndi awiri a Danieli" (Danieli 9:24-27). Mneneri Danieli adapatsidwa vumbulutso kuchokera kwa Mulungu lomwe adalinena masabata makumi asanu ndi awiri kwa zaka zambirimbiri zomwe adanenera kwa anthu ake, ayuda. Masabata makumi asanu ndi limodzi, kudzanso mphamvvu zisanu nzinai adakwaniritsidwa

pamemene Yesu Khristu adafika ku Yerusaalemu kutangotsdala sabata imodz kuti apachikidwe. Masabata makumi awiri adzakhala zaka zisanu ndi ziwiri za nthawi ya Israeli zomwe zizayambire pa mkwatulo kufikira kubweranso kwachiwiri.

E. Kubweranso Kwachiwiri

Kubweranso kwa chiwiri kukuimira kudzanso kwa Khristu patangotha miliri ya zaka zisanu ndi ziwiri (Mateyu 24:29). Zikusiyana ndi mkwatulo pakuti pakubweranso kwa chiwiri Yesu adzapondanso pa dziko lapansili (Zekariya 14:1-6) pamene pa mkwatulo adzangofikira mlengalenga (Machitidwa 1:11).

Iyi ndi nthawi imene adzagonjetse adani ake onse nkuyamba ulamuliro wa zaka chikwi (Chivumbulutso 19:20; 20:6). Khristu adzayamba waponda pa phiri la azitona, ndipo philiro lidzagawanika pakati ndipo adzapulumutsa okhulupilira a mu Israeli (Zekaliya 14:1-6). Adzayankhura nkuononga mfumu ya kumadzulo (2 Atesalonika 2:8; Chivumbulutso 19:15). Ndipo adzabweretsa moto kuchokera kumwamba nadzaononga mfumu yaku mpoto (Ezekieli 1:38-39) pomwe waononga kale mfumu yakumwera (Danieli 11:40-44). Iye adzagonjetsa maufumu aku m'mawa pamaso pawo (Yesaya 63:1-6; Chivumbulutso 14:20).

F. Ufumu kwa zaka Chikwi

Ufumu kwa zaka chikwi ndiwo ulamuliro wa Yesu Khristu pa dziko lapansi atabweranso kachiwiri. Pali magawo ambiri a mau omwe mumapezeka zizindikiro za ufumu umenewu.

Ufumuwu udzakwaniritsa kulonjezedwa kwa Abraham, Davide ndi pangano chatsopano; ndiponso kudzachotsa thembelero la munda wa Edeni (Genesis 33:17-19).

Zizindikiro zooneka ndi maso za ufumuwu ndi izi; (1) kutha kwa nkhondo (Yesaya 2:4; Mika 4:3); (2) padzakhala ubale wabwino pakati pa zinyama ingakhale zolusa (Yesaya 11:6-9; 35:9; 65:25); (3) sipazakhala mthenda kapena kupuwala zonse zidzachotsedwa ndipo nthawi yokhala idzaonjezeredwa (Yesaya 29:17-19); (4) sikuzakhala kuponderezedwa ku moyo, chuma komanso za ndale (Yesaya 14:3-6): (5) anthu adzachuluka (Yeremiya 30:20); (6) ntchito (Yeremiya 31:15; Yesaya 62:8-9, 23); (7) kutukuka kapena kukwera pa chuma (Yesaya 35:1, 27); ndi (8) kuwala kuchokera kwa ambuye (Zekaliya 14:6-7). Ufumu wa zaka chikwi uzakhuza a yuda ndi amitundu omwe adapilira chisautso ngati nkhosa (Mateyu 25:31-46). Kotero sikuzakhala anthu obadwa ndi uchimo pa nthawi ya ulamuliro wa zaka chikwi. Ana obadwawo sadzafunika kuti apulumutsidwe.

Zizindikiro za uzimu ndi izi: (1) ungwiro (Malaki 4:2; Masalmo 89:14); (2) kudziwitso chonsnse cha pa ambuye (Yesaya 11:9); (3) kuzadzidwa ndi mzzimu woyera (Yoweri 2:28-29); (4) chimwemwe (Yesaya 9:3-4); (5) chilungamo (Yesaya 9:7; 11:5; 32:16; 42:1-4; 65:25).

Ulamuliro wa Khristu udzakhala kwa onse (Daniele 7:14; Mika 4:1-2; Zefaniya 3:9-10; Masalimo 72:8) ndi boma limodzi (Ezekiele 37:24-28). Mlandu udzachotsedweratu (Masalimo 72:1-4; Chibvumbulutso 19:15). Yerusalem adzakhala likulu la dziko lonse (Yesaya 2:2-4; Jeremiya 31:6; Mika 4:1; Zefaniya 2:10-11) ndipo lidzatetezedwa ndi ya Mulungu (Yesaya 11:9). Lidzakhala losavuta kupeza (Yesaya 35:8-9) ndikukulitsidwa kwa kwakukulu (Jeremiya 31:38-40; Ezekieli 48:30; Zechariya 14:10). Yerusalemu adzakhalanso pachimake popembedzera (Jeremiya 30:16-21; 31:6, 23; Joweli 3:17; Zechariya 8:8, 20), adakhazikitsidwa mu mkachisis wa zaka chikwi cha kulamulira kwa Yesu pa dziko (Ezekieli 40:1–46:24) ndipo umatsogoleledwa ndi Zadoki ansembe a levi (Ezekieli 43:19; 44:15).

G. Mpando wa Chifumu wa Chiwreuzo

Mpando wa chifumu wa chiweruzo udzawoneka mu zaka chikwi za kulamulira kwa Yesu pa dziko lapansi komanso pamene satana adzamasulidwa pang'ono azaloledwa kudzasocheretsa a mitundu ndi kutsogolera "Agoge ndi Magoge," kudzaukira (Chibvumbulutso 20:7-8). Onse okhalamo a ufumu wa wa khristu pa dziko amene sanapulumutsidwe adzakhala olamulidwa. Ambuye adzathetsa mazunzo onse a satana potumiza moto kuchokera kumwamba ndi kumponya mu Nyanja yofiira ndi aneneri onyenga (Chibvumbulutso 20:9-10).

Pakutha pa zochitika zonsezo, osakhulupilira azaukisidwa kuti alandire chiweruzo chawo chomaliza pa "mpando waukulu woyera wachifumu wa chiweruzo." Adzaponyedwa mu ng'anjo yamoto (Chivumbuluso 20:11-15).

H. Kukhala mu Nthawi ya Zanthawi

Ili ndi tsiku limene limatchedwa "Tsiku la Mulungu" (2 Petro 3:12). Lidzayamba patangotha chiweruzo chochitika pa mpando waukulu woyera wa ufumu wa chiweruzo ndi kuononga kwa kumwamba ndi pansi pano ndinso kulenga kwa kumwamba ndi pansi pano kwa tsopano (Yesaya 65:17; 66:22; 2 Petro 3:12-13; Chivumbulutso 21:1). Dziko lapansi latsopanoli ndilo lidzakhale ndi Yerusalemu (Chivumbuluso 21:2-5)

zomwe zimakumbukira mitundu ya Israeli khumi ndi awiri ndi atumwi khumi ndi awiri. Simuzakhala kachisi mu yerusalemu watsopanoyu chifukwa Yesu Khristu nkhosa azakhala kachisi wake. Sikuzakhalanso dzuwa kapena mwezi pakuti nyali yake ndi nkhosa (Chivumbulutso 21:22-23). Mtsinje odzadza ndi "madzi amoyo" amene adzachokera ku mpando wa chifumu, ndinso "mtengo wa moyo" adzapange mtsinje kutulutsa zipatso zosiyanasiyana khumi ndi ziwiri, chilichonse mwezi wakewake (Chivumbuluso 22:1-2) sikudzakhala ntchito ku nthawi ya za nthawi (Chivumbulutso 21:24-27). Amene sanakhulupilire Yesu Khristu ndikulandira chikhululuko cha machimo awo sazaloledwa kulowa mu yelusalemu watsopanoyu. Adzakhala moyo wawo onse mu ng'anjo yamoto (Chivumbulutso 21:8). Okhawo amene "adzagonjetse" adzaloledwa kulowa ku moyo osatha ndi Mulungu wa moyo. Ulemu upite kwa Mulungu kuti ***"chikhulupiliro ndi kupambana komwe kumagonjetsa dziko!"*** (Yohane 5:4-5).

Dziwani kuti si tchimo lofotokozedwa mu chivumbulutso 21:8, limene lingakulepheretse kulowa kumwamba koma kulephera kukhulupilira Yesu Khristu ndi kukhululukidwa machimo.

Zoyenera kuchita aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Mutu 7, Gawo 5

1. **Werengani Aheberi 7:12. Kodi chinachitika ndi chani pamene kusandulika kwa zinthu kunachitika?**

2. **Werengani 1 Atesalonika 4:14-17 kodi okhulupilira adzakomana pamalo ati ndi Khristu panthawi ya mkwatulo?**

3. **Werengani 1 Akolinto 15: 51-52 , Kodi ndi nthawi yofulumira yotani imene mkwatulo wa mpingo udzachitike?**

4. **Werengani Yohane 14:1-3 kodi mpingo udzakhala kuti pamene nkwatulo udzathe?**

5. **Werengani Daniele 9:24-27 masabata makumi asanu ndi awiri amuzaka zisanu ndi ziwiri sanakwanilitsidwe. Kodi nthawi imeneyi imatchulidwa kuti chani?**

6. **Werengani Chibvumbulutso 19:11-16, Mateyu 24:29-30, komanso Zakariya 14:1-6, kodi Khrisitu adzachita chiyani pamene nthawi yachisautso yatha?**

7. **Kodi kusiyana kwakukuru pakati pa nkwatulo ndi kudza kwachiwiri kwa Yesu ndi kotani pokhudzana ndi n'thawi yake m'mene izi zonse zikuchitikira?**

8. **Werengani Chibvumbulutso 19:20, komanso 20:10 kodi ndindani adzaponyedwa mu Nyanja ya moto pakudza kwake kwachiwiri.**

9. **Werengani Chibvumbulotso 20:1-3. Kodi ndindani adzaponyedwe ku mphompho pakudza kwake kwachiwiri?**

10. **Werengani Chibvumbulutso 20:4-6. Kodi ufumu wa Khrisitu udzakhala nthawi yaitali bwanji pa dziko lino lapansi?**

11. **Werengani Chibvumbulutso 20:7-10 zitatha zaka chikwi, satana adzamasulidwa kwa kanthawi, nadzasokeretsa anthu, ndikugonjetsedwanso kodi pamapeto ake azonse adzaikhala kuti?**

12. **Werengani Chibvumbulutso 20:11-15 Kodi onse amene maina awo sanalembedwe mu "Bukhu la Moyo" chitatha chiweruzo ku mpando Woyera wachifumu adathera kuti?**

13. **Werengani 2 Petro 3:10-13, Chivumbulutso 21:1. Ndipo mulongosole kuti ndi chiyani chomwe chidzachitike pampando Woyera Wachifumu?**

Chaputala 8

Chiphunzitso cha Cholinga cha Mulungu

Gawo 1
Moyo wa Umunthu wa Khristu (Hodology)

A. Chiyambi

Cholinga cha Mulungu pa wina aliyense ndikuti asinthidwe kukhala chifaniziro cha Mwana wake Yesu Khristu (Aroma 8:29). Anakhazikitsa magulu awiri mu moyo wa munthu kuti akwaniritse cholinga chake m'miyoyo kudzera mu kusinthasintha kumeneku kudzatchulidwa ndime 1, 2 ndinso 3.

Ndime yoyamba imachitika pamene osakhulupilira wayamba kukhulupilira (Machitidwe 16:31). Iyi ndi nthawi imenemunthu amalandira chipulumutso.

Ndime yachiwiri ndi ndondomeko imene imachitika mwa munthu kuchokera pamene walandira chipulumutso kufika imfa.

Ndime yachitatu imayamba pamene imfa yakuthupi yachitika ndi kupitilira mpaka muyaya.

Kusintha koyenelera kupita ku chifanifani cha Yesu sikuzakwanilitsidwa pokhapokha titalowa ndime yachitatu, koma okhulupilira adzayamba kusintha nthawi ya chipulumutso (2 Akorinto 3:18). Chifanifani cha Yesu ndi umboni wokhala ndi maganizo ngati Mwana wake, wina ndi osazikonda, wodzichepetsa ndi opereka nsembe (Afilipi 2:5-8). Kusintha uku ndi mbali ya momwe, ***"tikuyendera mu njira ya maitanidwe"*** (Aefeso 4:1-3).

Zoti m'moyo wa okhulupilira muli magawo ndi chofunikira kuzindikira chifukwa chizathandiza okhulupilira mau a Mulungu. Tikafuza funso loti "ndani" tiyenera kuzindikira kuti Mulungu akuyankhula kwa okhulupilira ndi osakhulupilira ndi cholinga choti atanthauzire bwino uthenga. Sungani izi m'maganizo mwanu pamene tikuona za u zimu.

B. Zinthu Khumi ndi Zitatu za Moyo wa U Zimu

1. Chikhulupiliro

Chikhulupiliro ndikudalira winawake kapena chinachake. Ndichikhulupiliro chakuti wina kapena chinachake chikwaniritsa chokhumba chako. Chimene kapena amene timukhuliupilira ndiye chinthu chopambana osati chikhulupilirocho pachokha. Wina atha kuganiza ndikukhulupilira kuti munthu atha kulenga kumwamba ndi pansi ngati komwe timakhalaku koma palibe mphamvu zokwanira mwa munthu nkukwaniritsa kulenga. Chikhulupiliro chimenechi nchopanda ntchito.

Chikhulupiliro ndi chimene chimakhala ndikuthekera kokwaniritsa zinthu. Chikhulupiliro chathu chili mwa Mulungu amene analenga kumwamba ndi dziko lapansi chifukwa ali ndi kuthekera. Mau amati, ***"koma chikhulupiliro ndicho chikhazikitso cha zinthu zosayembekezeka. Pakuti momwemo akulu anachitidwa umboni ndi chikhulupiliro tizindikira kuti maiko ndi am'mwamba omwe anakonzedwa ndi mau a Mulungu, kotero kuti zinthu zopenyeka sizinapangidwe kuchokera mwa zoonekazo"*** (Ahebri 11:1-3).

Chikhulupiliro mwa Yesu ndi madziko a kukhululukidwa komanso kuyeretsedwa ndiponso chiyambi kapena njira imene talowera muchisomo cha Mulungu chimene chapelekedwa kwa munthu (Aroma 5:1-2). Chikhulupiliro nchofunikira kwa osakhulupilira kuti ayambe kukhulupilira pa ndime 1. Chikhulupilirochinso chimayambitsa ubale wathu ndi mzimu woyera (Agalatiya 3:22-3, 14).

Chikhulupiliro nchofunikira pa moyo wa uzimu (ndime 2) poti ndizosatheka kusangalatsa Mulungu popanda icho (Ahebri 11:6; 2 Akorinto 5:7). Mulungu amakondwera akachipeza chikhulupiliro mwa ife (Mateyu 8:5-10). Chikhulupiliro ndi chomwe chimapambana dziko, malinga a Satana (1 Yohane 5:4-5). Chikhulupiliro cha Khristu chizayesedwa kufuna kuona kukhwima kwathu mchikhulupiliro (Yakobo 1:3). Kakhalidwe ka chikhulupiliro chathu kamatipangitsa ife kukuza ubale wathu ndi Mzimu Woyera (Agalatiya 3:4-5). Chikhulupiliro ndi madziko pa moyo wa chi Khristu (2 Petro 1:5-9).

Tikadzakhala ndi Mulungu mpaka na muayaya m'matupi athu oukisidwa sipazafunikanso chikhulupiliro poti tidzamuona m'mene alili (1 Yohane 3:2).

2. Uzimu

Uzimu ndi mawu amene amaonetsa ubale umene ulipo pakati pa munthu ndi Mzimu Woyera. Ziyenera zitengere kudalira kwathu kwa Mzimu Woyera m'moyo. Osakhulupilira alibe ubale ndi Mzimu Woyera (1 Akorinto 2:14) ndipo alibe mulingo uliwonse wa uzimu.

a. Kokhala

Okhulupilira apano amasiyana ndi akale mwakuti kale Mzimu Woyera ankaagwirira ntchito pa okhulupilira ndipo masiku ano amagwira ntchito mwa iwo molingana ndi mau a Yesu khristu (Yohane 14:17). kupezeka kwa Mzimu Woyera mwa munthu ndi umboni wachipulumutso (Aroma 8:9).

Kukhala kwa Mzimu woyera mwa munthu ndi mphatso yopatsidwa kwa munthuyo pamene akulandira chipulumutso (Aroma 5v5; Machitidwe 11:16-17; 1 Akorinto 2:12). ndipo mphatso siingalandilidwe (Aroma 11:29). Chifukwa cha ichi Mzimu Woyera samachoka pamene munthu wachimwa. Izi zimakwaniritsidwa ngakhale panali Akorinto omwe anali akuthupi (1 Akorinto 3:3) ndi okhuzidwa mu uchimo (1 Akorrinto 5:5) komabe onse anali kachisi wa Mulungu oti mzimu agonemo (Akorinto 3:16; 6:19).

b. Kudzadza

Pamene uzimu utanthauza mulingo wa ubale wathu ndi Mzimu woyera, kudzazidwa ndi Mzimu Woyera ndi kuyamba kwa uzimu wathu. Tifunefune kuti tidzazidwe ndipo kenako adzatipatsa mphamvu zoti tithe kubala "chipatso" mwa ife (Agalatiya 5:22-23).

Kudzazidwa ndi mzimu woyera kunayambitsidwa m'malemba ngati kupereka mphamvu za paderadera kuti tithe kuchita ntchito zathu, m'moyo wa Chikhristu okhazikika. Ubwino oyamba odzazidwa ndi mzimu woyera unaoneka koyamba ndi stephano amene anasankhidwa kuti athandizire akazi wamasiye (Machitidwe 6:5). Kamvetsetsedwe kotereka ka tanthauzo la uzimu kofunika maka tikamaganiza kuti mpingo unayamba ngati Mwana kenako umalimbikitsidwa kuti ukule (Aefeso 4:11-16).

Kupatula mabuku anayi a uthenga wabwino ndi buku la machitidwe a atumwi nkhani yokhuza ndi kuzazidwa Mzimu woyera imakambidwanso ndi mtumwi Paulo yekha amene akupeleka lamulo kuti ***"ndipo musaledzere naye: inyo m'mene muli nchikaiko komatu mudzale naye mzimu"*** (Aefeso 5:18). Mau awa amaonetsa zimene zimachitika pozadzidwa ndi Mzimu Woyera chifukwa munthu saledzera pompopompo ndi vinyo. Ndondomekoyi inaphunzisidwanso m'mau oyambilira a Paulo "kudzadza" (PLELOO mu chi Greek), omwe amapezeka mu Aefeso 1:23; 3:19 ndinso 4:10. Lamulo la Paulo limanena ubwino wa kudzazidwa ndi Mzimu Woyera zomwe zimakhuza kuzindikira ndinso kulapa machismo, kukhulupilira kuti Mulungu watikhululukira. kufunika kwa kuchilimika kumaonetsanso kuti nkofanana ndi mzimu wathu.

Uzimu weniweni umakhudza chisomo ndi chikhulupiliro. Tidauzidwa kuti ***"monga momwe munalandira khristu Yesu Ambuye, Muyende wa iye ozika mizu ndi omangirika mwa iye, ndi okhazikika m'chikhulupiliro , monga munaphunzitsidwa ndi kuchulukitsa chiyamiko"*** (Akolose 2:6-7). Tinamulandira iye kudzera mu chikhulupiliro (Aefeso 2:8-9). Tinaphunzitsidwanso bwino kuti moyo wa uzimu umene umatsogolera kukhwima mu chikhristu wazikidwa mu kueynda m'chikhupiliro (Agalatiya 3:2-3) ndipo kupanda chikhulupiliro nkosatheka kusangalatsa Ambuye (Ahebri 11:6).

Pomaliza kudzazidwa ndi mzimu woyera kumapereka mphamvu kwa okhulupilira choncho adzakhala okhwima mwa Yesu Khristu.

c. Kukhumudzitsa ndi kudzimitsa

okhulupilira akachimwa, zimamukhumudzitsa kapena kubweretsa chisoni kwa Mzimu Woyera (Aefeso 4:30). pamene tchimoli likhala osalapidwa mwa okhulupilira, Mzimu Woyera amakhalabe okhumudwa. Mau awa akufotokoza m'mene zimakhalira m'moyo mwa okhulupilira.

Okhulupilira akadzimitsa Mzimu Woyera, monga momwe munthu amadzimitsira moto, zikutanthauza kuti waononga moyo wake wa uzimu kapena chipatso cha mzimu woyera mmoyo wake omwe kapena wa mzake (1 Atesalonika 5:19) Sitiyetsera kuimitsa mzimu woyera akamagwira ntchito mwa okhulupilira.

3. Kuvomereza Machimo

Pamene zadziwika kuchokera mu Mawu a Mulungu kuti tikapulumutsidwa, ndiye kuti machimo athu akhululukidwa, koma ndizachidziwikirenso kuti ngakhale tiri okhulupilira tingadzachimwenso (Aroma 7:14-25). Uchimo, sinkhaninso pa chipulumutso chathu, koma pa moyo wathu wa chikhristu. Uchimo mu moyo wa okhulupilira, umavulaza ubale wake ndi Mulungu ndi anthu enanso, koma sumathetsa ubalewo, choncho tchimo limakhala vuto pa chiyanjano chathu.

Chiyanjano chimatanthauza, kugawana wina ndi mzake. Kugawanaku, kukuimilira anthu, zochitika, zinthu, komanso nthawi. Ngakhalle osakhulupilira, angathe kukhala pa chiyanjano wina ndi mzake mu kuchita uchimo. Pamenene munthu wokhulupilira kaya wosakhulupilira, aphwanya malamulo a chiyanjano, amabweretsa mkwiyo pakati pa wina ndi mzake. Monga akhristu, tiyenera kukhala mu chiyanjano ndi Mulungu, ndi wina ndi mnzake, monga ana a Mulungu. Choncho ndi chiyanjano chomwe chiri ndi maziko a choonadi chomwe Mulungu anakhazikitsa.

Uthenga wa momwe tingabwezeretsedwere mu chiyanjano ndi Mulungu ndi akhristu ena chakambidwa kale pa 1 Yohane 1:5-10.

Pa vesi 5, akulongosola muyeso wa chiyanjano kuti ***"Uwu ndiwo uthenga womwe taumva kuchokera kwa Iye, ndipo tikuwulengeza kwa inu, kuti Mulungu ndiye kuunika, ndipo mwa Iye mulibe mdima"*** Muyezowo ndi wakuti, kuwala kwa Mulungu, ndiko choonadi chake pa ochimwa.

Vesi 6 ikunena za mayeso a chiyanjano kuti ***"Tikanena kuti tiyanjana naye koma tikuyendabe mu mdima, tidzinyenga tokha,ndipo mwaife mulibe choonadi."*** Kusonyeza kuti mu malingaliro, malankhulidwe ndi zochita zathu, tiyenera kuyesedwa mayeso ndi kuunika kwa Mulungu**.**

Vesi 7 ikunena za malamulowo/zofunika kuchita mu chiyanjano kuti ***"Koma ngati tiyenda mu kuunika monga Iye mwini ali mu Kuunika, tiri pa chiyanjano wina ndi mnzake, ndipo mwazi wa Yesu mwana wake utiyeretsa kutisambitsa ku uchimo wonse."*** Malingaliro athu, zolankhula ndi zochita zathu, ngati ziri zofanana ndi za Khristu, zidzabweretsa chiyanjano pakati pathu, komanso kupitilira kutiyeretsa ku uchimo.

Vesi 8 ikutionetsera poyera za chimo kuti ***"Tikanena kuti tiribe uchimo, tidzinyenga tokha, ndipo mwa ife mulibe choonadi"*** Mawu oti "Ti" akunena za okhulupilira onse, kuphatikiza Yohane Mlembiyo. Choncho, ngati tikuganiza kuti sitingachimwenso, tikungozinyenga tokha.

Vesi 9 Ikutipatsa yankho ku uchimo, ndipo akuti ***"Koma ngati tivomereza ndi pakamwa pathu machismo athu, Iye ali okhulupirika ndi olungama kutikhululukira ndi kutiyeretsa pa chisalungamo chonse."*** Mawu oti "Kulapa" anachokera mu chigiriki (HOMOLOGEO) Kutanthauza kuvomereza, kulolera kwathu, kumuuza Mulungu kuti zoonadi ndachimwa pa zolankhula, zoganiza ndi zochita. Zindikirani kuti Mulungu adzatikhululukira pokhapokha ngati kuvomereza kwathu kuli kolapadi osangoti kungonena chabe. Mulungu sanyengeka (Agalatiya 6:7). Mulungu adzakukhululukirani, ngati mwamukhulupilira huti angathe kutero ndipo mawu awa muziwagwiritsa ntchito nthawi zonse.

Vesi 10 ikulongosola za onse omwe sakumazindindikira uchimo, ndipo ikuti ***"Tikanena kuti sitinachimwe, timupanga Iye kukhala wabodza, ndipo mawu ake sali mwa ife."*** Apa vesili, likunena kuti, ngati sitizindikira ndi kuvomereza kuti tchimo lilipodi pa miyoyo ya akhristu, tikusonyeza kuti Mulungu ndi wabodza ndipo mawu ake sakuwamvetsa Mulunguyo.

Tikaphatikiza ma vesi onsewa pamodzi, tipeza kuti, Chiyanjano chathu chauzimu ndi Mulungu (Vesi 6),ndi okhulupilira ena (Vesi 7) chavulazidwa ndi uchimo. Tchimo ili likufunikira livomerezedwe pamaso pa Mulungu (Vesi 9) (Mulungu wathu ndi wokhulupilika ndi wolungama) ndipo potero, chikhululukiro chidzachitika, komanso chiyanjano chathu chidzabwezeretsedwa.

Chonde, zindikirani kuti mavuto ndi zotsatira za uchimo za muyaya ndi zomwe Mulungu anakhululukira. Okhulupilira angathe kuonabe mavuto ena pa nthawi posatira zimene iye amachita. Adamu ndi Hava, anakhululukiridwa, komabe Mulungu anawachotsa mu munda wa Edeni.

4. Mphatso za Mzimu

Mphatso za Mzimu ndi kuthekera kopatsidwa ndi Mulungu kuti tikwaniritse kuchita zinthu zina mu "Thupi la Khristu." Mawuwa, akuchokera mu mawu a mu Chigiriki oti (CHARISMA). Mphatso ndi zosiyana ndi talenti (maluso) yomwe imadza pachibadwa mokhazikitsidwa nd Ambuye (Aefenso 4:11) ndipo M,zimu Woyera amagawa mphatsotsozo pa nthawi ya chipulumutso (1 Akorinto 12:11-18) ku thupi la Khristu (Aefenso 2:20). Munthu aliyense ali ndi mphatso, pafupifupi imodzi (1 Petro 4:10) koma osati mphatso zonse. Kuopa angakhale thupi lonse payekha (1 Akorinto 12).

Ndi chofunika kuzindikira kuti Mphatso zonso zikugwira ntchito mu Chikondi (1 Akorinto 13) ndipo zinakonzedwa kuti zitumikire ena (1 Petro 4:10). Mtumwi Paulo ananena mwa chimvekere mu 1 Akorinto kuti, ngakhale zili mphatso za Mzimu zopatsidwa ndi Mzimu woyera, zingathe kugwiritsidwa ntchito moipa kuthupi kwa mwini mphatsozo, kapena kuzitamandira nazo (1 Akorinto 12). Mphatso za uzimu zimathandiza kumanga mpingo osati kudzetsa mpatuko ndi chisokonezo (1 Akorinto 14:12, 33).

Pali malo asanu mu chipangano chatsopano momwe mphatso za Mzimu zatchulidwa maina, imodzi imodzi **(1 Akorinto 12:8-10)**. Tikuona Mawu a Nzeru, mawu a chidziwitso, chikhulupiliro, machiritso, zozizwa, mauneneri, chidziwitso, kuzindikiritsa mawu, malilime ndi mamasulilidwe a malilime. Mu **1 Akorinto 12:28**, tikuona Atumwi, Aneneri, Aphunzitsi, Zozizwa, Kuthandiza, Kukonza zinthu ndi Malilime. Mu **Aefenso 4:11** tikuona Atumwi, Aneneri, Alaliki, Aphunzitsi, ndi Abusa. Mu **1 Petro 4:11** kulumikizana ndi ntchito, zaperekedwa monga magulu awiri a mphatso za Mzimu. **Aroma 12:6-8** akutipatsa mdandanda wa mphatso za Mzimu.

Chonde, zindikirani kuti Mphatso za Mzimu zinaperekedwa ku mpingo omwe unayamba pa tsiku la Pentekoste (Machitidwe 2). Mphatso zina zinaikidwa kuti ziyale maziko (Aefenso 2:20) kuti Mpingo uyambe, umangidwe, ndi kukhazikika (1 Akorinto 14:40). Mphatsozi, zinkatchedwa 'ZIZINDIKIRO' kapena 'Mphatso za Zizindikiro' ndipo ntchito yake inali yolalikira osakhulupilira kuti asandulike kukhala okhulupilira atsopano (1 Akorinto 14:20-22). Mpaka nyengo yosintha mphatsozo zinali zosafunikira itatha nyengoyo chifukwa zinakwaniritsa kugwira ntchito zonse za mu mpingo woyamba (1Akorinto 13:8-10).

Nayi ndondomeko yosonyeza mphatso za Mzimu za kanthawi kochepa zomwe sizikugwiranso ntchito mu nyengo ino.

Mphatso za Mzimu za Nthawi Yochepa (Tempurare)	
Mawu a Nzeru (1 Akorinto 12:8)	Malangizo ozama oyenera kugwiritsa ntchito pa mpingo oyambirira
Mphatso ya Chikhulupiliro (1Akorinto 12:9)	Kukhulupilira Ambuye mozama, angakhale mu nyengo zosatheka ndi zowawitsa
Mphatso ya Chidziwitso (1 Akorinto 12:8)	Kuthekera kumva mawu kuchokera kwa Ambuye, kupita ku Mpingo, osati mwa uneneri, mpaka chipangano chatsopano chinatha kulembedwa.
Machiritso (1Akorinto 12:9, 28)	Machiritso a pompopompo, a matenda osiyanasiyana popanda mankhwala.
Zozizwa (1 Akorinto 12:10, 28)	Kukhazikitsidwa kwa Mawu ndi mfundo zomwe zimaturutsa ziwanda, kuchiza ndi kugwira ntchito zosiyanasiyana.
Mauneneri (1 Akorinto 12:10, 28; Aroma 12:6; Aefenso 4:11)	Mphatso yapadera yodziwiratu ndi kunena zomwe zizachitike ku mpingo nthawi ya mtsogolo
Mphatso Yozindikira Mizimu (1 Akorinto 12:10, 28)	Mphatso yozama, yozindikiritsa Aneneri, Aphunzitsi onyenga, ndi oona (1 Akorinto 14:32)
Malilime/ Ziyankhulo zina (1 Akorinto 12:10, 28)	Kuthekera kozama kolankhula chiyankhulo chomwe sunmachiphunzirepo
Kumasulilidwa Malilime/ Ziyankhulo zina (1 Akorinto 2:10)	Kuthekera kozama komasulira malilime ndi ziyankhulo
Utumwi (1 Akorinto 12:28; Aefenso 4:11)	Mphatso yozama yomwe inaperekedwa kwa ophunzira oyamba aja khumi ndi awiri, okhawo (Chivumbulutso 21:14) omwe anakhala ndi Yesu (Luka 6:13-16; Machitidwe 9:15; Agalatiya 1:1)

Tikuphunziranso kuti "Mauneneri," "Malilime" ndi "mawu achidziwitso," adzatha woyerayo akadzafika (1 Akorinto 13:8-10). Ndipo akadzatha awa, "Kuzindikira mizimu" ndi "kumasulira malilime" sizizaonekanso chifukwa zimagwira ntchito molumikizana ndi mphatso zitatuzi. Mphatso ya nzeru, ndi ya chikhulupiliro, Zikuonekanso kuti zimagwira ntchito pamodzi ndi zinzake zomwe zinathazi. Choncho, zindikirani kuti, mphatso zonsezi zikulumikizana pogwira ntchito zawo. Mmene bukhu la chivumbulutso limalembedwa, uneneri unatsekedwa mu zaka za mpingo woyamba (Chibvumbulutso 22:18-19). Choncho, "Woyerayo" anatsiriza kulemba mawu owuziridwa ndi mpweya wa Mulungu, ndipo palibe nkhani yatsopano yomwe imafunikanso kuwonjezera pa chibvumbulutso. Mphatso ya Uphunzitsi inali yongolumikizitsa pa zomwe mawu a Mulungu aulula za chipangano chatsopano.

Chibvumbulutso 21:14 akutisonyeza kuti panali Atumwi Khumi ndi Awiri Okha. Ngati pali anthu otchedwa Atumwi lero, sizikusonyeza kuti iwowa ali nayo mphatso ya utumwi (Agalatiya 1:19 M'bale wake wa Yesu anali m'modzi mwa Atumwi enieniwo). Ndipo izi zikusonyeza kuti, Mphatso ya utumwi inali ya nthawi yochepa.

Mphatso ya "Machiritso" ndi "Zozizwa," zinali za kanthawi kochepa monga tikunenera mu chipangano chatsopano. Yesu angathe kuchiza anthu ndi kuchita zozizwa koma kudzera mu mphatso yoperekedwa kwa munthu. Ambuye akuyankhabe mapepemphero mpakana lero (Yakobo 5:16). Koma ntchito ya mphatsoyi imatengera kukhala nayo. Okhala ndi mphatso ya Machiritso, amaitanira pa Ambuye ndipo odwalawo amachira (Machitidwe 3:6-8; 5:12-16; 9:34). Mphatsozi zinali kugwiritsidwa ntchito mu mpingo woyamba kuti zikope anthu kumva uthenga wa kuukanso mmanda kwa Yesu Khristu (Machitidwe 8:1-8, 39; 13:4-12; 14:1-4; 19:11-12). Chikondi cha okhulupilira, pa wina ndi mzake, ndi njira yozama tsopano, yotengera anthu ku chikoka, ku uthenga wa Yesu Khristu (Yohane 13:34-35).

Tikudziwa kuti Mtumwi Paulo, anali ndi mphatso ya machiritso (Machitidwe 20:8-12; 28:8) pomwenso nthawi Ina iyeyo analephera kuchiza mnzake wapamtima Epafrodito (Afilipi 2:25-27), komanso iye mwini (2 Akorinto 12:7-9). Podziwa kuti mphatsoyi inali itawachokera atumwiwo, anthu omwe anayamba nawo mpingo woyamba, zikuonetsanso kuti mphatsozi zinamuchokera wina aliyense.

Mphatso zina zinapangidwa kugwirra ntchito ku mpingo utachoka pa msinkhu, ukhanda (1 Akorinto 13:10-13). Choncho, mphatso zotsatirazi ndi zamuyaya ndipo cholinga chake ndi kufalitsa mawu a Mulungu pofuna kutumikira ena (1 Petro 4:10-11).

Ndondomeko iyi ikufotokoza mphatso zamuyayazi (zosasinthazi) zimene zizagwiritsidwebe ntchito mpaka lero.

Mphatso Zosatha ku Mpingo	
Uphunzitsi (1 Akorinto 12:28; Aroma 12:7)	Kuthekera kolumikizana ndi anthu powatumikira Mawu a Mulungu.
Zachifundo (1 Akorinto 12:28)	Mphatso yapadera yothandiza ena ovutika ndi osowa.Monga kutolera ndi kugawa zakudya kwa ozisowa (Machitidwe 6:1-6)
Dongosolo Labwino (1 Akorinto 12:28)	Mphatso, yoyang'anira ndi kusonkhanitsa zinthu zomwe Mulungu wapereka ku mpingo.
Kutumikira Ena (Aroma 12:7; 1 Petro 4:11)	Mphatso yosamalira ndi kutumukira ena pa zosowa zakuthupi, mu utumiki
Malangizo/ Ulangizi (Aroma 12:8)	Mphatso yozindikira ndikufikira zosowa za anthu mowalimbikitsa monga thupi la khristu.
Kupatsa (Aroma 12:8)	Kukwanitsa kuthandiza osowa kuuzimu kapena kuthupi.
Kutsogolera (Aroma 12:8)	Kukwanitsa kutsogolera anthu pa zochitika mu utumika.
Chifundo (Aroma 12:8)	Kukwanitsa kutsogolera anthu pa zochitika mu utumiki
Ulaliki (Aefeso 4:11)	Kukwanitsa kupereka uthenga wabwino wa Yesu Khristu, kwa anthu momveka bwino, kuti akhulupilire ndi kutembenuka mtima.
M'busa-Mphunzitsi (Aefeso 4:11)	Mphatso yokwanitsa kusonkhanitsa pamodzi nkhosa za Mulungu kudzera mu chiphunzitso ndi mu mawu.

5. Chilungamo

Mu ndime yathayi, taona kuti Mulungu anatipatsa chilungamo pamene tidakhulupilira mwa Yesu Khristu. Ichi chimatchedwa "Chilungamitso." Wokhulupilira watsopano amakumana ndi 'zipsinjo' ndi cholinga choti azame mu uzimu ndikudziwa chabwino ndi choipa. Chilungamo mu moyo wa wokhulupilira chimaima pa machitidwe ake osasinthika molingana ndi miyezo ya Mulungu.

Miyezo iwiri yopambana kwambiri ya chilungamo ndiyo "Kukonda Mulungu ndi mtima wako wonse, ndi kukonda anzako monga iwe mwini" (Marko 12:29-31). Chilungamo sikusapezapeka kokha kwa uchimo ayi, koma kusinthika mu malingaliro molingana ndi mgwirizano ndi Mulungu (Afilipi 2:5-8). Mwachitsanzo, tiyenera ***"Kukhala achifundo, popeza Atate wathu ndi wachifundo, komanso tikonde adani athu"*** (Luka 6:36-40), ndipo titurutse zipatso zabwino kuchokera mu chilungamochi, pothandiza osowa onse mwa chisomo cha Mulungu (2 Akorinto 9:8-10). Ntchito zogwirizana ndi chifuniro cha Mulungu ndiyo mbali imodzi ya choonadi (Ahebri 11:32-33).

Chilungamo cha wokhulupilira chiyenera kutsatidwa kapena kulondoledwa (1 Timoteo 6:11; 2 Timoteo 2:22-23). Mawu onse a Mulungu ndi ofunika kwa munthu kuti amveketse za chilungamo ichi (2 Timoteo 3:16-17), ndipo, chifukwa cha chimenechi, ndikovutilapo kuti munthu amene wangokhulupilira kapena kubadwa kumene mwatsopano amvetsetse ndi kulandira (Ahebri 5:12-14).

Mogwirizana ndi muyeso wa Mulungu pokhuzana ndi chilungamo (chilungamo) si kungomvera zolamula za Mulungu ndicholinga chosangalatsa anthu (Mateyu 6:1). Afarisi anali ndi 'Chilungamo chawo' moti aliyense amawadziwa nacho. Komanso anali ndi zikhulupiliro zina za kuthupi zomwe iwo amaziphatikiza ndi mawu a Mulungu (Marko 7:1-8) choncho, munthu akachoka mu mawu a Mulungu ndikumati ali mu choonadi, izi zimatchedwa 'Chikunja,' (LEGALISM) Ndipo icho sichoonadi chomwe Mulungu akufuna pa ife.

Mzimu Woyera umatsutsa munthu aliyense wosowa chilungamo (Yohane 16:8-10), kwa osakhulupilira, Mzimu woyera amaululira kuti kusapanga choonadi kuzamulepheretsa kukhala pa ubale ndi Mulungu woyerayo. Mwa chikhulupiliro, Mdzina la Yesu Khristu, wokhulupilira, amapulumutsidwa (Aefenso 2:8-9) ndipo akalengezedwa mu chilungamo, angathe kukhala pa chiyanjano ndi Mulungu. Wokhulupilira amatsutsidwa ku uchimo, ndipo amalozeredwa ku kulapa machimo kuti chiyanjano chake ndi Mulungu chibwezeretsedwe (1 Yohane 1:6-10). Choonadi chimadza ndi Mzimu Woyera, ndipo ndi chofunika pa moyo wa mu ufumu wa Mulungu (Aroma 14:16-17). Choonadichi, ndi mphatso yochokera ku kuunikwa kwa Yesu Khristu yemwe anakhala woyerabe mu miyezo yonse.(Aefenso 5:6-10).

Yesu akutiuza kuti, tikamva njala ya Chilungamo, tidzakhuta (Mateyu 5:6). Tiyenera kukhumba chilungamo, chifukwa chimalemekeza yemwe anaukitsa ife ku imfa ya uzimu (Aroma 6:12-13). Osakhulupilira ndi akufa mu uzimu, mpaka nthawi yomwe avomereza Khristu kukhala Mpulumutsi wawo (Aroma 6:23). Pamene tinali osakhulupilira, tinali akapolo a chimo, koma popeza tiri okhulupilira, tiri akapolo a chilungamo (Aroma 6:16-19).

Satana ndi amithenga ake, amaziika okha ngati akapolo a chilungamo, ongofuna kunamiza anthu okhulupilira (2 Akorinto 11:13-15). Ndipo njira yomwe amagwiritsa ntchito ndi yozunza omwe ali mu moyo wa chilungamo (Mateyu 5:10; 1 Petro 3:14). Kuti tikhale a chilungamo ndi nkhondo ndithu, koma pamapeto pake tidzalandira kolona wa Muyaya (2 Timoteyo 4:6-8). Tiyeni tsono tiphunzitsidwe ndi Ambuye pa nthawi ya nkhondoyi, ndipo tizindikire mtendere weniweni mu miyoyo yathu (Ahebri 12:11).

6. Pemphero

Pemphero ndi kulumikizana ndi Mulungu. Kungodziwa kuganizira kapena kuphunzira za pemphero kokha kulibe phindu. Koma kuchita pempherolo, ndipo limakhala ndi phindu ngati mwapemphera ndi kudikira yankho kwa Mulungu. Ndipo ndi lofunikira chifukwa limatsegula khomo lolowera pa mpando wachifumu wa Mulungu (Ahebri 4:16).

Kukhazikika pa Pemphero, ndiwo mankhwala a iwo omudalira Mulungu mu moyo wawo. Izi zinalinso chomwecho ku Mpingo woyamba (Machitidwe 2:42). Pamene ophunzira a Yesu anamupempha kuti awaphunzitse kupemphera (Luka 11:2),Yesu anawaphunzitsa iwo "Pemphero la a Mbuye" (Luka 11:2-4). Chinsinsi cha pemphero si ndicho kusankha mawu othyakuka ayi, koma kuyankhula ndi kufuna chifuniro cha Mulungu ndi iwe mwini, ndi kuziphatika mu chifunirocho (1 Yohane 5:14). Pemphero ndi lofunikira, angakhale pakati pa makangano ndi angelo (Aefenso 6:18).

Mawu a Mulungu akutiuza kuti, pemphero liyenera kupita kwa Atate (Aefenso 5:20; Mateyu 6:9; 1 Petro 1:17), mu mphamvu ya Mzimu Woyera (Aefenso 6:18), ndipo lizithera mu dzina la Mwana Wake, Yesu Khristu (Yohane 14:13; 15:16).

Pemphero likhale ndi mafungulo asanu: (1) Kuvomereza ndi kulapa machimo (Masalimo 66:18-20; Yesaya 59:2; Mateyu 6:14; 1 Yohane 1:9). Polingalira kuti china chake chasokonezeka, chiyanjano chathu ndi Mulungu; (2) Matamando (Mateyu 21:16; Luka 19:37; Aroma 14:11; Aroma 15:11; Aefenso 1:6, 12, 14; Ahebri 13:15); (3) Chiyamiko /chithokozo. Uku ndi kuthokoza ndi kuzindikira zinthu zonse zomwe Mulungu watichitira pa moyo wathu (1 Atesalonika 5:18); (4) Mapembedzero, kutanthauza kupempherera anthu ena (Aefenso 6:18; Ahebri 7:25); ndi (5) Kupempha/kuzipempherera wekha/kupempha zosowa zako kuti Mulungu akupatse (Ahebri 4:16).

Mungathe kulapa, kapena kupempha, kapena kupembedzera, pa nthawi iriyonse yomwe mwasankha.

7. Kukula

Chimodzimodzi tikamabadwa mu dziko, monga khanda, tikabadwa mwatsopano, (Yohane 3:1-16) timayenera kukhala mu chikhristu. Ndipo mpaka timazama, ndiye popeza kukula ndi kokonzedwa ndi Atate wa Kumwamba (Mateyu 5:48) sikumatha pa moyo uno (Afilipi 3:12-15).

Chinthu choyamba pa kukula ndicho' Kodi tidzafikira pamaso pake monga "Nsembe yamoyo ndi yoyera" (Aroma 12:1-2) kapena ayi? Atate athu amaika mayeso osiyanasiyana otithandiza kuti "Tikule"

(Yakobo 1:2-4) ndipo awa ndi mayeso a chikhulupiliro chathu komanso amapereka mphatso za Mzimu kuti zithandize pa kukula (Aefenso 4:11-14).

Kukhwima mu uzimu ndiko ***"Kusiya zinthu zachibwana"*** (1 Akorinto 13:11). Munthu wokhwima msinkhu, amachita zinthu zazikulu (Mateyu 19:21), mu mayankhulidwe (Yakobo 3:1-2), maganizo (1 Akorinto 14:20). Tingadziwe za kukhwima kwathu kudzera mu zimeneze, popeza ntchito za khanda ndizo Kuzikonda, kuchita zoipa, miseche, kuzikuza, madano, kufuna kutchuka.

Popeza wina akamafuna kutchuka, iyeyu ndi khanda, sanakhwime. Pali zoyenereza pa kukhwima mu uzimu. Monga kusazikonda wekha (Mateyu 19:21), kuzichepetsa (Afilipi 3:12-15), ulaliki (Akolose 1:28), kupembezera ena (1 Akolose 4:12), ndi kugwiritsa ntchito uzimu mwa ulemu, mosalilira phindu kapena kutchuka (Yakobo 1:28; Agalatiya 5:1, 13). Kukhwima kumasonyeza kuti munthu akuyamikira muyeso wa chilungamo wa Mulungu (Ahebri 5:12-14), ndipo kuti, Munthuyo amadalira pa chisomo cha Mulungu (2 Akorinto 12:9) Pozindikira kuti zabwino zonse zimachokera ku chisomo cha Mulungu (Yakobo 1:17). Okhwima mu uzimu, amakhala pa Chikondi ndi chiyanjano ndi Mulungu, ndipo amakhala opanda mantha pa moyo uno (1 Yohane 4:17-19).

8. Chikondi

Yesu Khristu mwini anati, "Chikondi ndi chofunika pa moyo wa mkhristu aliyense" Mu bukhu la Marko, Yesu anatenga mawu a pa Deutoronomu 6:4-5, ndi kuwaika kukhala lamulo lalikulu kuposa onse, ndipo iye anati, ***"Lamulo lalikulu loposa onse ndi ili; Lemekeza Israeli, Ambuye Mulungu ndi M'modzi, ndipo uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi Mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zonse, ndi mphamvu zako zonse"*** (Marko 12:29-30). Ndipo anatenga lamulo lachiwiri, kuchokera pa Levitiko 19:18, ndipo anati ***"Lachiwiri ndi ili, Uzikonda anzako monga uzikonda iwe mwini, palibenso ena oposa awa"*** (Marko 12:31). Tiyenera kumukonda Iye chifukwa anatikonda ife koyamba (1Yohane 4:19), ndipo tikamukonda Iye, tikondanso abale athu (1 Yohane 4:20-21). Chikondi chomwe chikufunika, sichapakamwa ayi, koma cha pansi pa mtima chochokera kwa Mzimu Woyera (Agalatiya 5:22).

Chikondichi, chimalongosoledwa bwino ndi mawu a Mulungu. Ndime ya 1 Akorinto 13, yayamba ndi kutiphunzitsa za kufunika kwake. Zilibe kanthu kutu tiri ndi mphatso ya Mzimu yotani, koma ngati tiribe Chikondi, ife tiri chabe pa moyo wa chikhristu ndi pamaso pa Mulungu (1 Akorinto 13:1-13). Mtumwi Paulo, akulongosola maonekedwe okwana 16 a chikondi (1 Akorinto 13:4-8). Kuti muzidziwe nokha, pofunika muzifunse nokha kuti kodi ine ndiri ndi zomwe zalembedwazi? Ngati yankho liri ayi, ndiye kuti mulibe Chikondi. Malongosoledwe enanso a Chikondi, alembedwa pa Aroma 12:9-21.

Dziko lapansi', ndi mdani wa Chikondi, chomwe Mulungu akuchifuna mwa ife. Dziko lapansi' limaimilira, zinthu zomwe Satana amazigwiritsa ntchito polakalaka kukhotetsa ife kutichotsa ife ku chifuniro cha Mulungu. Ngati ife tikonda zinthu za padziko, sitingakonde Mulungu kwa thunthu (1 Yohane 2:15).

9. Mazunzo / Masautso

Mazunzo akutanthauza kukumana ndi zopweteka pa moyo. Zingathe kukhala zooneka kapena zosaoneka, za mu malingaliro. Mwa Yesu Khristu, tikuona kuti, Iye anakumana ndi mazunzo pamoyo wake, pofuna kulupila dipo la machismo athu pa mtanda (1 Petro 2:21-24; 4:1, 5:1) Iye anadza padziko ndicholinga (Luka 9:22; 22:15). Ndipo Iye anazunzidwa ndi anthu opanda chilungamowo (1 Petro 2:21-24). Choncho, kuchokera pa Iye, titengereponso chitsanzo kuti ifenso tizazunzidwa ndi anthu osakhulupilirawo (1 Petro 2:21).

Koyamba kuja, tinafotokoza za kukula mu moyo wa chikhristu. Kuzunzika ndi mbali ina ya mayeso omwe timadutsamo kuti tikhwime mu uzimu (1 Petro 5:10). Mulungu adzapereka mphoto kwa umboni wathu ndi chipiliro chathu (1 Petro 2:19-20; 2 Akorinto 4:17). Umboni wathu wakhazikika pa chidaliro chathu mwa iye pa nthawi ya msautso (1 Petro 4:19).

Ndi mdalitso, kusautsika chifukwa cha chilungamo pokakamira kuchita chilungamo, pozindikira kuti Khristu ndiye Ambuye (1 Petro 3:14-17; 4:14). Chisautsocho chimadza kuchokera kwa anthu amene ndi amaudindo, pofuna kuletsa munthu kukhulupilira Khristu. Ndipo ndi chofunikira kwambiri popeza mkhristu, kudzera mu msautso, amasunthidwa kuchokera muyezo wina kufika muyezo wina (Afilipi 1:27-30).

Mtumwi Petro, yemwe anachitira umboni mazuzo a Yesu Khristu (1 Petro 5:1) akutiuza kuti' 'Tichiyese chimwemwe pokumana ndi masautso' (1 Petro 4:13-16). Podziwa kuti ngati dziko likudana ndi Khristu, lizadananso ndi ife omutsatira ake (Yohane 15:18-20; 1 Petro 4:12). Ndi masautso a Yesu Khristu okha omwe anapereka dipo pa machimo athu, masautso a ife athu sangakwanitse. Tisadere nkhawa kuti ndi

masautso otani tikukumana nawo (1 Petro 4:16), Koma tizindikire kuti akhristu anzathu anapilira mu masautso (1 Petro 5:9), ndipo akwanira pa muyezo wa ufumu wa Mulungu (2 Atesalonika 1:5), choncho, tisamaope masautso (Chibvumbulutso 2:10).

Petro anachenjezanso kuti, pamene tisautsika, pa tchimo lomwe talichita, tiyenera kuvomereza chisautsocho, chifukwa sichoyenera mu moyo wa chikhristu (1 Petro 4:15). Tchimo liri lonse, liri ndi zotsatira/ mphoto yake (Luka 13:1-5).

10. Kudzudzula /Chidzudzulo

Mawu oti chidzudzulo (PAEDEUO mu chi Giriki) akuimilira ganizo lobweretsa chowawa kuti munthu alangike, atengerepo phunziro. Mwa chitsanzo mu Luka 23:16-23, anagwiritsa ntchito pomumenya wandendeyo, kuti asinthike. Ndipo wandendeyo anali Khristu, ndipo Pilato ankafuna kuti akasintha mayankhulidwe, amumasule. Chidzudzulo, chimabweranso ngati chiphunzitso (Machitidwe 7:22; 22:3). Ambuye akatiika mu gulu la okhulupila oyamba aja, tiyenera kuphunzitsa modekha (2 Timoteo 2:24-26).

Chidzudzulo, chimafanana ndi chisautso, popeza zonsezi zimabweretsa kupweteka, koma chisautso chimangofuna kukonza kuti ufike pa muyezo wina, pomwe chidzudzulo chimangophunzitsa pofuna kuti usinthe (1 Timoteo 1:18-20).

Chidzudzulo cha Mulungu chiri monga abambo amaphunzitsa mwana wawo (Aefenso 6:4; Ahebri 12:7). Chinapangidwa mu njira yoti imangirire, kukhazikika mu malingaliro a chilungamo, ndi mu mawu onse a Mulungu (2 Timoteo 3:16-17). Sichachimwemwe kapena sizimakoma panthawi yomwe mukulandira chidzudzulo. Koma pakutha pa chidzudzulo, mumasinthika ndipo mumapindula (Ahebri 12:11). Dipo lomwe Yesu analipira pa machimo athu, lititsogolere ife pa kufunika kwa chiphunzitsochi (Tito 2:11-12).

Mosiyana ndi abambo akudziko, omwe amadzudzula ndi mkwiyo, Mulungu amadzudzula ndi Chikondi chake (Chibvumbulutso 3:19) Iye amatiphunzitsa chifukwa choti amatikonda. Choncho, tisadere nkhawa kapena kukhumudwitsika ngati akutidzudzula (Ahebri 12:5). Cholinga cha Mulungu pakutidzudzula ndi choti, tisamachite zinthu monga anthu ochimwawo (1 Akorinto 11:31-32). Choncho, okhulupilira ayenera kulandira chidzudzulo cha Ambuye (Ahebri 12:8).

11. Kuphunzira Baibulo

Kufunika kowerenga baibulo ndi chinthu chomwe sitingathe kuchichepetsa. Ndi kofunika ndithu. Baibulo ndi bukhu lokhalo lomwe likutitsogolera ku ubale wathu ndi Mulungu (1 Akorinto 2:16). Choncho liyenera kuwerengedwa tsiku ndi tsiku.

12. Kulambira

Kulambira ndiko kukondwerera za Yesu Khristu. Umu timanenamo zomwe Yesu ali, ndi zomwe watichitira, komanso kuvomereza ndi kuyamikira pa zomwe Iye ali. Ndi Yesu yekha woyenera (Chibvumbulutso 5:1-7). Ndipo kumwamba kuzazindikirika ndi kulambira ambuye (Chibvumbulutso 4:9-11).

Anthu osakhulupilira, amapembeza ndi kukhulupilira zolengedwa kuposa Mlengiyo (Aroma 1:25). Satana mwini amafunanso kupembezedwa (Luka 4:7), koma Mulungu ndi yekhayo woyenera kupembezedwa (Luka 4:8). Ena amapembeza angelo, zolengedwa zina za Mulungu (Akolose 2:18). Ndipo ena amapembeza timalamulo tomwe anakhazikitasa okha (Marko 7:7). Ena amapembeza malo opemphereramo, koposa Ambuye (Yohane 4:20-22).

Kupembeza koona kumachokera kwa Mzimu Woyera akugwira ntchito mu miyoyo yathu, povomereza kuti Yesu Khristu ndiye woyenera (Yohane 4:23-24; Afilipi 3:2-3), kuti amupembeze Iye. Kupembeza kumachitika popereka matupi athu kwa Iye, mwa chikhulupiliro, ndi kuvomereza mawu ake (Aroma 12:1-2; Ahebri 11:21).

Ngakhale pali njira zambiri zopembeza, tiyenera ife kutsata njira yomwe mawu a Mulungu aphunzitsa chifukwa kumuweruza munthu uzimu wake, kaya kukhwima kwake mu uzimu ndi “Chikunja.”

13. Kulalikira /Kukhala ndi Akuphunzira

Kutuma kwa Yesu Khristu, Iye anawauza ophunzira ake kuti ***“Pitani, mukalalikire uthenga wabwino, ophunzira ku maiko onse”*** (Mateyu 28:18). Ophunzira, ndi munthu yemwe akuphunzira mawu a Mulungu, ndipo wasankha kumutsata Ambuye Yesu Khristu. Wophunzira siwongopulumutsidwa kokha ayi, koma ndiye wophunzira yemwe akukhulupiliranso Mawu a Mulungu kuti akhale mu mawuwo kapena kuwachita mawuwo (Yohane 7:17).

Zoyenera kuchita aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Mutu 8, Gawo 1

1. **Mokhuzana ndi mawu a moyo wa chikhristu:**
   a. Werengani machitidwe 16:30-31. Ndi ziti pa moyo wa munthu zomwe zimachitika pamene wakhulupilira mwa Mwa Yesu Khristu?
   b. 2 Akorinto 3:18. Ndi ziti pa moyo wa munthu zimachitika pofuna kusintha munthu kukhala m'maonekedwe a Mkhristu?
   c. 1 Yohane 3:2. Ndi ziti zomwe zidzachitika akadzamuona Khristu monga Khristu alili?

2. **Werengani Ahebri 11:6. Kodi okhulupilira akhale ndi chiyani, kuti akondweretse Mulungu?**

3. **Werengani 1 Akorinto 2:14-18. Chofunika ndi chiyani kuti timvesetse zinthu za uzimu?**
   a. Werengani Yohane 14:17. Kodi Mzimu Woyera amakhala kuti?
   b. Werengani Agalatiya 3:2-3. Chofunikira pa uzimu ndi chiyani?
   c. Werengani Aefenso 4:30 ndi 1 Atesalonika 5:19. Tchulani zinthu ziwiri zomwe tchimo limabweretsa pa okhulupilira?

4. **Werengani 1 Yohane 1:5-10. Kodi wokhulupilira adzachimwanso? Nanga achite chiyani tsono?**

5. **Werengani 1 Petro 4:10. Okhulupilira adzalandira chiyani?**
   a. Werengani 1 Akorinto 13:1-3. Kodi payenera kuti pakhale chiyani kuti pakhalenso kupindula pamene okhulupilira agwiritsa ntchito mpahatso za mzimu?
   b. Werengani 1 Akorinto 13:8-11. Tikumva motani za zomwe zizachitike ku mphatso zina
   c. Werengani Yohane 13:34-35 ndi 1 Petro 4:10. Fanizirani cholinga chenicheni cha "kukondana wina ndi mzake' ndi chifukwa chomwe tinapatsidwira mphatso mphatso za mzimu?

6. **Werengani Aroma 6:16-19. Tiyenera kukhala akapolo ku chiyani?**

7. **Pokhuzana ndi zinthu 5 zofunika mu pemphero**
   a. Werengani 1 Yohane 1:9. Akunena za chiyani?
   b. Werengani Aroma 14:11 ndi 15:11. Akunena za chiyani
   c. Werengani 1 Atesalonika 5:18. Akunena za chiyani?
   d. Werengani Aefenso 6:18. Akunena za chiyani?
   e. Werengani Ahebri 4:16. Akunena za chiyani?

8. **Werengani 1 Petro 2:2 ndi 2 Petro 3:18. kodi mkhrisitu achite chiyani akapulumutsidwa?**

9. **Werengani Marko 12:29-31. Tchulani malamulo a akulu awiri a Mulungu?**

10. **Werengani 1 Petro 2:19-20, 5:10. Kodi okhulupilira ayenera kupilira pa chiyani?**

11. **Werengani Ahebri 12:6-7. Kodi Mulungu amatiphunzitsa kudzera mu njira iti?**

12. **Werengani 2 Timoteo 3:16-17. Kuphunzira Mawu a Mulungu, kuli ndi phindu lanji?**

13. **Werengani Yohane 4:23-24 ndi Afilipi 3:2-3. Tizipembeza motani?**

14. **Werengani Mateyu 28:18-20. Ophunzira a Khristu adzichita chiyani?**

Gawo 2
Moyo Womangililika wa Chikhristu (Ecclesiology)

A. Chiphunzitso

Pamene Yesu anawalamulira ophunzira ake, gawo lina la malangizo linali ***"Kuphunzitsa onse achite zomwe analamula"*** (Mateyu 28:20). Yesu anali Mphunzitsi (Mateyu 4:23; 5:2; 7:29; 9:35; 11:1; 13:54; 21:23; 22:16; 26:55; 28:15; Machitidwe 1:1). Ophunzira ake anachita zomwe Iye anawalamulira ndipo anayamba kuphunzitsa (Machitidwe 4:2, 18; 5:21, 25, 28, 42; 11:26; 15:1, 35; 18:11, 25; 20:20; 21:21, 28).

Chiphunzitso chimatipatsa malangizo pomwe ulaliki umalimbikitsa (Akolose 1:28; 3:16). zonse ziwirizi ndizofunika ku mpingo.

Pamene mtumwi Paulo anapereka malangizo kwa Timoteo, Iye anawauza iwo kuti aphunzitse anthu ena kuti potero athenso kuphunzitsa ena (1 Timoteo 4:11; 6:2; 2 Timoteo 2:2). Umu ndi momwe mawu a Mulungu amayendera kuchokera mbadwo wina kufika wina.

Anthu ena ali ndi Mphatso ya Mphunzitsi (Aroma 12:7), koma okhulupilira onse akufunsidwa kuti aphunzitse (Ahebri 5:12-14).

B. Chiyanjano / Kusonkhano Pamodzi

Kusonkhana pamodzi kunali kofunika kwambiri pa mpingo woyamba (Machitidwe 2:42). Mu kusonkhanaku, amagawana chirichonse angakhale ndi zinthu zathupi (Aroma 15:26; 2 Akorinto 8:4; 9:13; Ahebri 13:16). Komanso za uzimu (1 Yohane 1:3, 7). Mu kusonkhana pamodzi analinso kupembeza monga talongosolera mu ndime 1 ya ya chaputala chino. Kupembedza Ambuye pamodzi mu chiyanjano kumachokera ku kukula ndi moyo wakulambira Mulungu kwa mu nthu aliyense payekhapayekha.

Chiyanjano cha uzimu ndi okhulupilira (2 Akorinto 6:14) chakhazikika pa kuyanjayana naye Yesu Khristu (1 Yohane 1:7) ndipo kwaperekedwa kudzera mu kuyanjana naye Mzimu Woyera (2 Akorinto 13:14), komangiriridwa mu chikhulupiliro (Filimoni 1:6), ndipo kumabweretsa umodzi mu thupi la Khristu (Alilipi 2:1-2) Tikufunsidwa kuyanjana (1 Akorinto 1:9), ndipo chiyanjano mu mazunzo ake (1 Yohane 1:6).

Maziko a chiyanjano chathu ali kuwonetseredwa pagome, otchedwa 'Mgonero' omwe umatikumbutsa za umunthu ndi ntchito ya Khristu (1 Akorinto 10:16) ndipo zamangiririka ndi chiyanjano mu mazunzo ake (Afilipi 3:10)

Monga okhulupilira tiri pa chiyanjano, tikachoka pa kusagwirizana (Agalatiya 2:9) ndipo titayamba kugwira ntchito pamodzi yofalitsa uthenga wabwino (Afilipi 1:5). Chiyanjano ndi njira yomwe kukondana ndi maubale zinakhazikitsidwa.

Taona kuchiyambi kuti Chikondi ndi chofunika pa moyo wa mkhristu. Tiyenera kukonda Mulungu komanso kukonda anzathu, momwe Mulungu afunira (1 Yohane 4:20). Kukonda mzako monga iwe mwini kumachedwa 'Lamulo la chifumu' (Yakobo 2:8). Uwu ndi muyeso wa Chikondi cha okhulupilira ndipo tikuuzidwanso zoti tikonde adani athu (Luka 6:35). Tichitire anthu zomwe ife tingakonde atatichitira (Mateyu 7:12).

Izi ndi mfundo za momwe tingachitire ubale wathu ndi ena. Kuyambira m'mbanja, ubale mpaka pa madzi, mu mpingo, banja la Mulungu ngakhalenso osapulumutsidwa. Pali mfundo zochuruka mu chipangano chatsopano zomanga chiyanjano. Wokhulupilira wosakhwima adzayembekeza kuti anthu ena amuchitire iye ali chete. Koma wokhwima adzachitira izi anthu ena pozindikira kuti Mulungu akumulamula kuti azitere.

Tiyeni tiganizire mfundo yoti "Wina ndi mzake":

- Langizo lokondana wina ndi mzake likupezeka malo ambiri mu chipangano chatsopano (Yohane 13:34, 35; 15:12, 17; Aroma 13:8; 1 Atesalonika 3:12; 4:9; 2 Atesalonika 1:3; 1 Petro 1:22; 1 Yohane 3:11, 23; 4:7, 11, 12; 2 Yohane 1:5). Izi zikusonyeza kuti tiyenera kukhala mu makhalidwe a mu 1 Akorinto 13:4-8 ndi Aroma 12:9-21).
- Zindikirani kuti, ndife ziwalo za wina ndimzake (Aroma 12:5; Aefenso 4:25) Kusonyeza kuti tiri pa chiyanjano kale chifukwa ndife thupi la Khristu.
- Tiyenera kudzipereka kwa wina ndi mzake (Aroma 12:10) kusonyezakuti tilolerane ndikuchitirana zinthu zabwino.
- Tilemekezane wina ndi mzake kusonyeze kuti anzathu ndi ofunikira pamaso pa Maulungu (Aroma 12:10).

- Tiganize mofanana pa wina ndi mzake, kusonyeza kuti tivomereze anzathu popeza iwenso analandira chisomo cha Mulungu (Aroma 12:16;15:5).
- Tivomerezane wina ndi mzake monga Khristu anativomera ife (Aroma 5:7), monga zolengedwa zosowekera chisomo chake.
- Tichenjezane wina ndi mzake, tikaone zoopsa ziri kudza (Aroma 15:14).
- Tipatsane Malonje wina ndi mzake (Aroma 16:16; 1 Akorinto 16:20; 2 Akorinto 13:12; 1 Petro 5:14), ndi "Mpsopsono Woyera" kusonyeza kulemekeza kuti munthu aliyense ndiwofunika pamaso pa Mulungu.
- Titumikirane wina ndi mzake (Yohane 13:14; Agalatiya 5:13) zomwe zikuonetseredwa posambitsa mapazi.
- Tione anzathu ofunika koposa ife (Afilipi 2:3).
- Tisenzerane zolemetsa (Agalatiya 6:2), kuthandizana kuthana ndi uchimo ndi zovuta pa moyo.
- Tilolerane wina ndi mzake, tifatse pa anzathu (Aefenso 4:2; Akolose 3:13).
- Tizipereke kwa wina ndi mzake, kusonyeza kuika zosowa za ena patsogolo kuposa zathu (Aefenso 5:21).
- Tilimbikatsane wina ndi mzake kusonyeza kuti kuthandizana akamagwa kuuzimu (Aroma 1:12; 1 Atesalonika 4:18; 5:11; Ahebri 3:13; 10:25).
- Tikhale ochitirana mtendere wina ndi mzake (Marko 9:50). Tisasonkhezera mavuto pa ena.
- Tilape machismo athu (Yakobo 5:16).Tipite kwa omwe tawalakwira ndikuwapepesa, ndipo iwonso atikhululukire.
- Tipempherane wina ndi mzane (Yakobo 5:16).
- Tikhululukirane monganso Ambuye anatikhululukira (Akolose 3:13).
- Tikhumbe zabwino kwa wina ndi mnzake, tifunisitse aliyense atakhala wa Mulungu (1 Atesalonika 5:15).
- Titakasane wina ndi mzake kuchikondi ndi ntchito zabwino (Ahebri 10:24).
- Tidikirane wina ndi mzake (1 Akorinto 11:33), tikhale mu chiyanjano ndi chimwemwe.
- Tiyenera tikhale achifundo wina ndi mzake zomwe zimakhuza kuchotsa zowawa, nkwiyo komanso nkhumbo loipa kwa ena (Aefenso 4:31-32).
- Tisamalirane wina ndi mzake (1 Akorinto 12:25), tikhazikitsidwe ndi mamembala ena a thupi la Khristu.
- Tivomerezane wina ndi mzake (Luka 7:32), tithandizane poganizira kuti tikutumikira Mulungu osati Munthu.
- Ticheze ndi alendo (1 Petro 4:9), tilandire bwino alendo panyumba ndi kumpingo.
- Tizichepetse pamaso pa wina ndi mzake (1 Petro 5:5).
- Tikhale pa chiyanjano/ tisonkhane pamodzi (1 Yohane 1:7).
- Timangilirane wina ndi mzake (Aroma 14:19; 1 Atesalonika 5:11), tilimbikitsane ndi kulangizana.

C. Kufalitsa uthenga wabwino

Ulaliki ndi kufalitsa uthenga wabwino wa Yesu Khristu. Uku ndi ndiko kunena zakuti alipire dipo lowombola dziko ku uchimo (Yohane 1:1) yemwe anadza monga munthu (Yohane 1:14), kuti alipire dipo lowombola dziko ku chimo (1 Yohane 2:1-2), ndipo atafa anauka (1 Akorinto 15:1-3), kuti onse okhulupilira iye, akhale nawo moyo wosatha (Yohane 3:16). Uwu siuthenga wabwino onena kuti tonse ndife ochimwa (Aroma 6:23). uthenga wabwino ndiwonena kuti ngongole yomwe tinali nayo chifukwa cha machimo athu inaperekedwa ndi Yesu (Agalatiya 3:13).

Mpingo uyenera kufunisitsa kubweretsa uthenga wabwino. Sitiyenera kubisa kuunika ndi choonadi chomwe tinachilandira (Mateyu 5:14; Aroma 1:16).

Mulungu amatipatsa ufulu kuti tipereke uthengawu. Tingapereke uthengawu kuchoka pa munthu mmodzi kukafikira kwa wina (Machitidwe 8) kapena pagulu (Machitidwe 2). Chofunikira ndicho kuti mpingo ufalitse uthenga wabwino. Chida cha ulaliki ndi chikondi pa wina ndi mzake (Yohane 13:34-35).

D. Utumiki

Utumiki umazindikira zosowa za uzimu, zakuthupi ndi za malingaliro, ndipo umafunisitsa kuthandiza pa zosowazo (Machitidwe 11:29; 2 Akorinto 8:3-5). Utumiki ndi ntchito yokhala kazembe wa Khristu ndi kutenga uthenga wa kukonzedwanso kwa dziko lomwe linavunda pachiyambi (2 Akorinto 5:18-21). Munthu akabwezeretsedwanso kwa Mulungu ndiye kuti wamasulidwa ku za mdziko. Choncho utumiki umanyamula uthenga wa bata ndi mtendere (1 Timoteo 4:4-6). Ife ngati okhulupilira tinamasulidwa (Agalatiya 5:1) ndipo tsopano tikugwiritsa ntchito ufulu kupulumutsa ena (Agalatiya 5:13).

Yesu Khristu iye yekha apereka chitsanzo kwa ife (Mateyu 20:28), choncho nduna imatsatira mtsogoleri (Yohane 12:24-26). Utumiki wa Uchikhristu suyang'ana udindo wa Mkachisi koma kutumikira ngati kapolo chicho chizindikiro chenicheni chanchikuru (Mateyu 20:26-28; 23:10-12). Ngati okhulupilira tayenera kumakumbukira nthawi zonse chifundo cha Mulungu potipatsa ife chipulumutso choncho sitifoka (2 Akorinto 4:1-2). Mulungu watilonjeza kuti sazayiwala ngakhalenso kunyoza ntchito zazing'ono za ife kwa anzathu (Ahebri 6:10-12).

Mwai wotumikira waperekedwa ndi Ambuye (Machitidwe 20:24; 1 Akorinto 12:4-6). Ndipo okhulupilira ayenera aulandire ndi kuwugwiritsa ntchito yotumikirana. Utumiki ndi mbali yofunikira pa moyo wa chikhristu (1 Petro 4:10-11) womwe tiyenera nthawi zonse kuwuchita (Aroma 12:7), mosamalitsa posaunyozesa komanso posanyoza Yesu Khristu (2 Akorinto 6:3).

Mautumiki aphunzire kugwira ntchito pamodzi. Masankho oyamba a Atumiki/Adikoni anali oti atumikire pa zosowa za mpingo. Atumwi anaona kuperewera pa kusamalira anthu kuthupi, ndipo anapempha amunawo/madikoni asamalire amasiye (Machitidwe 6:1-6). Ndipo ma utumiki osiyanasiyana atagwira ntchito pamodzi anathandiza kupereka zosowa za anthu kuthupi komanso ku uzimu.

Ambuye anakhazikitsa utsogoleri wa Mpingo kudzera mu mautumiki, ndipo Mtumwi Paulo anati,

> ***Ndipo kwa ena Atumwi, kwa ena Aneneri, ena Alaliki, Abusa, Aphunzitsi, kuti akakonzekeretse oyera mtima ku ntchito ya utumiki ndi kumangilira thupi la Khristu. Kufikira titakhala mu chiyanjano cha okhulupilira ndi chidziwitso cha Mwana wa Mulungu. Kufikira ku kukhwima pa muyezo ndi chikhalidwe cha chidzalo mwa Khristu*** (Aefenso 4:11-13).

Ntchito ya utsogoleri mu mpingo ndi kukonzekeretsa okhulupilira mu uzimu, kuthupi ndi malingaliro, kuti akatumikire ndi kulalikira ena kuti akhwime mu ubale wawo ndi Ambuye Yesu Khristu. Utumiki wochitidwa mu Chikondi ndi chida champhamvu wamphamvu cholalikilira kapena kufalitsa uthenga wabwino chimene chinapatsidwa ku mpingo (Yohane 13:1-35).

E. Umodzi

Mipingo payokha iyenera kukhala ndi cholinga cha umodzi mu thupi la Khristu (Aefenso 4:13). Yesu Khristu, usiku uja, asanapachikidwe anapemphera kuti omutsatira akhale amodzi, ndipo anati,

> ***Sindikupempha m'malo mwa awa okha, koma kuti okhulupilira enanso mwa ine, kudzera mu mawu, akhale amodzi, popeza inu Atate muli mwa ine, ndi Ine, mwa Inu, Kuti iwo akhale monganso Ife, kuti dziko likakhulupilire kuti munandituma Ine. Ndi kuti Ulemelero womwe munaupereka pa Ine, Inenso ndaupereka pa iwo, kuti akhale amodzi, monga Ife tiri Mmodzi. Ine mwa Inu, ndi Inu mwa Ine, kuti ayeretsedwe mu umodzi, kuti dziko likadzindikire kuti munandituma ine, kuti munawakonda iwo, komanso munandikonda ine*** (Yohane 17:20-23).

Pozindikira kuti Mzimu Woyera amagonera kapena kukhalira mwa okhulupilira onse, kuyambira nthawi yomwe akhulupilira Yesu Khristu, umodzi unakhazikitsidwa poyamba popeza pali Mzimu mmodzi (Aefenso 4:4) ndipo iye amakhalira mwa onsewo. Mtumwi Paulo anaphunzitsa za Umodzi wa Mzimu Woyera (Aefenso 4:1-3) kusonyeza kuti mayendedwe athu ndi odzadza ndi chisomo molingana ndi chikhulupiliro (Aefenso 8–9). Pomwe maimidwe athu mwa Khristu akutiyenereza kukhala mu chipulumutso, ndipo tiyenerera kufunafuna umodzi mu thupi la Khristu, womwe wagona pa Chikondi, ndi cholinga choti osatembenuka mtima, azindikire kuti ife, ndi ophunzira ake a Yesu Khristu (Yohane 13:34-35).

Zoyenera kuchita aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Mutu 8, Gawo 2

1. **Werengani 2 Timoteo 2:2. Tchulani kufunika kwa Mpingo?**

2. **Werengani 1 Timoteo 6:3. Kodi chiphunzitso cholamitsa tingachiunike bwanji?**

3. **Werengani Ahebri 5:12. Kodi anthu omwe akhala okhulupilira kwa nthawi yaitali akhoza kuchita chiyani?**

4. **Werengani 1 Yohane 1:3 ndi 7. Kodi chomwe chimaoneka chofunika kwambiri pa mpingo ndi chiyani?**

5. **Ndi ndondomeko ziti za chiyanjano zomwe zalongosoledwa mu ndimeyi?**
   a. Yohane 13:34-35
   b. Aroma 12:10
   c. Aroma 15:7
   d. Agalatiya 5:13
   e. Afilipi 2:3
   f. Agalatiya 6:2
   g. Ahebri 3:13 ndi 10:25
   h. Akolose 3:13
   i. Aefenso 4:31-32
   j. 1 Petro 4:7
   k. Aroma 14:19

6. **Werengani Mateyu 5:14 ndi Aroma 1:16. Kodi Mpingo uchite chiyani?**

7. **Werengani Agalatiya 5:1 ndi 5:13. Khristu anatimasula kuti tikhale mfulu chifukwa chiyani?**

8. **Werengani Aefenso 4:13. Kodi cholinga cha mpingo chizikhala chotani?**

9. **Werengani Yohane 17:20-23. Kodi cholinga cha Khristu pa omutsatira chinali chotani?**

Chaputala 9

Kugwiritsa Ntchito

Malonje

Ndime ino ilongosola za njira zoyenera pokonzekera maphunziro a Baibulo. Njira iyi yalongosoledwa mogwirizana ndi mfundo zomwe aphunzitsi ochuruka akhala akugwiritsa ntchito pophunzitsa Mawu a Mulungu. Ngakhale njira ziripo zosiyanasiyana, njira zachindunji zomasulilira mawu zomwe taphunzira mu chaputala 4, mukuyenera kudzitsatira mwa kuzigwiritsa ntchito.

Choyamba, lingalirani maphunziro a kusukulu, ndipo zindikirani kuti maphunziro a kusukulu asakujejemetseni pa kuphunzira za mawu a mulungu ndi za Mzimu woyera. Mzimu woyera ndiye yemwe ***"amatitsogolera ku choonadi"*** (Yohane 16:3) chomwecho, palibe njira yokonzedwa ndi munthu yomwe ingamutsogolele munthu ku choonadi.

Tiyenera kulankhula mwa chikhulupiliro, posatengera kuti tili ndi chidziwitso chochuluka bwanji cha mawu a Mulungu (Akolose 2:6). Kukhwima mu chikhristu sikumadza ku thupi ayi koma mu chikhulupiliro (Agalatiya 3:2-5). Satana adzayesayesa kukujejemetsani kuti muzingokhulupilira za nokha osati Mzimu Woyera (Yohane 5:39-47) chidziwitso cha Satana ndi chopanda chikondi, komabe izi zizakutsogolerani mu nkharwe, chomwe ndi chikhalidwe cha kusakhwima mu uzimu (1 Akorinto 8:1).

Zilibe kanthu, kuti tikufuna titachita chani moyo wa chikhristu, tiyenerabe kukhala pa pemphero komanso kuvomereza zolakwa zathu (1 Akorinto 11:3; Miyambo 28:3; 1 Yohane 1:9) ndiponso tipitilire kupemphera. Tipempherere chidwi, kumvetsa komanso kusunga zomwe taphunzira kale tisanayambe phunziro lina.

Gawo 1
Kufuna Kuzindikira Bukhu

A. Chidziwitso

Titasankha bukhu loti tiwerenge, tiyenera tiliwerenge kaye kangapo ngati kuti ndi news paper kapena buku lina lililonse. Izi zili chonchi chifukwa zimatithandizila ife kuti tiziwe zimene zalembedwa mbukhulo osati kuti tiyakhe mafunso ovuta a phunziro la bukhu.

Kuwerenga bukhu mwachangu kangapo kutinthandizira kuti tiziwe mfundo zina za mamphunzilo ofunikira komanso zolembedwa. Tiyenera kutanthaudzira zolembedwazo potengera zorembedwa zoyambilila komanso zakumapeto kuwerenga buku vesi ndi vesi ndi njira yokhayo imene ingatithandizire kuti timvetse zolembedwa zoyambilira ndi zotsatira zake.

Tiyeneranso kudziwa mbiri ndi malo amabuku osiyanasiyana a buku loyera. Phunziro ili litengera pa 1 atesalinika. Kuti tithandize ophunzira kulongosora za nzinda la Tesalonika. Zolongosolazo ziyenera kuti zitengedwe mu ma buku ena pambali pa buku loyera. Ma buku a matanthauzo a mawu a m'baibulo komanso mawu oyamba kapena malonje a buku lina liri lonse la buku loyera angathandizire kwambiri pa kulongosola za mbiri komanso malo amene zinthu zina zinachitikira.

B. Malo ndi Mbiri ya a Tesalonika

Tesalonika inali doko lomwe linali pamutu pa chilumba cha Temiki pa ngodya la ku mpoto cha kumadzulo kwa Nyanja ya Aegean ku dziko limene likudziwika kuti Greece masiku ano. Linakhazikisidwa mu dera la chiroma lotchedwa Macedoniya ndipo limadziwika ndi nyengo yake yotentha komanso kuti malo a sitima kumene ma sitima akuluakulu amapezekerako.

Tesalonika anakhazikitsidwa monga nzinda mchaka cha 315 B.C ndi Cassander, mwana wa Antipater, patangotha nthawi pang'ono mmene anamwalira Alexander wamkulu. Pambuyo pa kumwalira kwa Alexander panali kukanganinirana udindo. Antipatera anali wokhulupilika wakubanja la chifumu anautchula dzindawo dzina lake la mwana wake, Tesalonika, amene anali mchemwali wake wa Alexandera wamkulu.

Tesalonika linali dera la malonda lomwe linayamba ndi anthu a chigiliki koma linali dera la ayuda. Lero ndi dera la chi Giriki lotchedwa Salonika.

C. Kulongosora Mbiri ya Mpingo: Machitidwe 17:1-9

Mpingo unayambitsidwa pa ulendo wa utumiki wa Paulo wa chiwiri kutengera zotsatira za masomphenya (Machitidwe 16:9). Paulo anaperekezedwa ndi sila lomwe linali dzina la chi Hebri, Silvanus linali dzina lake la chi Roma, Timoteo ndi Luka. Amayenda munjira yomwe imalumikiza ndi kumadzulo. Gululi linafika ku tesalonika litafika m'dera monga Filipi, Amfipoli komanso Apoloniya (Machitidwe 17:1).

Paulo anaphunzitsa mu sinagoge kwa masabata atatu (Machitidwe 17:2) ndi uthenga onena kuti Yesu anakwaniritsa ulosi wa chipangano chakale komanso kuti iye anali mpulumutsi (Machitidwe 17:3). A mbiri anakopedwa chifukwa cha uthengawu (Machitidwe 17:4).

Paulo anakhalanso ndi nthawi ina yosakambidwa bwinobwino kuphunzitsa anthu okopedwa. Chifukwa cha ichi, a yuda osakhulupilira anakhala ansanje, ndipo anapanga gulu nayamba kutsatira anthu opemphera (Machitidwe 17:5). Gululo linapita ku nyumba ya yasoni kuti akamutenge Paulo amene sanali kumeneko (Machitidwe 17:6), ndiyeno anamutengera yasoni kubwalo ndipo kumeneko amanyoza utumiki wa Paulo okhuza za Yesu (Machitidwe 17:7). Anthu anavuta kwambiri mpaka Paulo ndi gulu lake anathawira ku Bereya (Machitidwe 17:8-10).

D. Nthawi Imene kalata ya Tesalonika inalembedwa Komanso Chifukwa Chake

Ulendo wa utumiki wa chiwiri unayamba mu chaka 49 Yesu atamwalira kalepamene Paulo anaphunzitsa pa antiyoki. Atachoka ku Atesalonika, Paulo anaphunzitsa ku bereya kenako ku Athena asanapite ku korinto kumene anakhala chaka chimodzi ndi miyezi isanu ndi umodzi (Machitidwe 18:11). Paulo anatumiza Timoteo ku Tesalonika kuti akaone m'mene Mpingo watsopano ukuyendera (1 Atesalonika 3:2). Uthenga wa Timoteo unali wabwino ndipo zosatira zake zinali bukuli. Izi zikutanthauza kuti Atesalonika linambedwa patadutsa zaka 50 Yesu atamwalira. Linari buku lachiwiri lomwe Paulo analemba (loyamba linari la Agalatiya).

Zoyenera kuchita aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Mutu 9, Gawo 1

Werengani nkani ya mu Chapter 3 yomwe ikunena za 2 Atesalonika

Gawo 2
Muyenera Kulongosora Buku

Pamene takonzeka kuti tisanthule buku, tiyenera tiyambe ndi kupanga ndandanda wa momwe bukulo ndi mitu yake zalembedwera. Choyenera kuchita ndikudziwa kapena kukhala ndi chithunzithunzi cha zomwe bukulo likukamba lonse, kenako tiwone zomwe zakambidwa monga mitu in'gonoin'gono komanso mitu ina yayin'gono pansi pa mitu inzake kapena magawo pansi pa mitu in'gonoin'gono. Ubwino wokhala ndi nthawi yakuyan'gana zonsezi ndi wakuti umakhala ndi kumvesetsetsa kwabwino. Mau a Mulungu ali ngati chonchonso. Nkhani yayikulu pamenepo ndiye Yesu Khristu mwini. Mau olembedwa ndi vumbulutso la mau a moyo (Yohane 5:39-47). Tikayang'anitsitsa tingathe kuona umunthu weniweni wa Khristu.

Sitiyenera kutanganidwa kwambiri ndi tsatanetsatane wa zinthu zambiri mpakana kufika polephera kuzindikira chachikulu chimene tayenera kuchidziwa. Ngati titero ***"tidzachotsa ka ntchentche mu chakumwa chathu koma ndikumeza Ngamira"*** (Mateyu 23:24) zimene zikuthandauza, tidzalephera kupeza zofunika kwambiri.

Pamene tikufuna kulongosora buku, ntchito yoyamba nkudziwa m'mene uthenga wagawiridwa m'ma gawo osiyanasiyana. Ambiri otanthauzira buku loyera ali ndi njira yoziwira magawidwe ake a mau. Nthawi zambiri, otanthauzira, amaona nambala ya vesi ndi yoyamba mu gawo la mau. Welengani chiziwitso cha chomwe mukutanthauziracho kuti muone m'mene otanthauzirayo anaonetsera magawo amau. Ngati magawowo sanaonetsedwe, pitilizanibe, koma mukuona m'mene kusintha kwa phunziro kukumachitikira.

Mwa chitsanzo, magawo a 1 Atesalonika ali chonchi;

1. 1:1
2. 1:2-10
3. 2:1-12
4. 2:13-16
5. 2:17-20
6. 3:1-10
7. 3:11-13
8. 4:1-8
9. 4:9-12
10. 4:13-18
11. 5:1-11
12. 5:12-22
13. 5:23-28

Kenako perekani dzina kapena mutu ku gawo lililonse la ndime. Pamene tikuwerenga bukhuli kwambiri, kulongosora kwathu kuzisintha pamene tikuona zolemba zambiri. Pa nthawiyi sitimaona kwambiri mainawo. Ntchito yathu nkufuna kudziwitsa koma mosavutitsa kwambiri.

Kulongosora kwa magawo a 1 Atesalonika kumaoneka chonchi:

1.	1:1	Kulandilidwa komanso kupasidwa ulemu
2.	1:2-10	Kuthokoza chifukwa cha chitsanzo chao
3.	2:1-12	Udindo wa Paulo
4.	2:13-16	Kuthokoza chifukwa chakusamala kwao
5.	22:17-20	Kufuna kwa Paulo kuti awaone iwo
6.	3:1-10	Kufuna kwa Paulo kuti aone m'mene akusunthira
7.	3:11-13	Chiyembekezo cha Paulo kuti akwele mu uzimu
8.	4:1-8	Kufuna kwa Paulo kuti ayeretsedwe
9.	4:9-12	Kuyankhura kwa Paulo pa chikondi chao
10.	4:13-18	Kufa kwa Khristu
11.	5:1-11	Tsiku la Yehova
12.	5:12-22	Malamulo ofunika kuchitidwa
13.	5:23-28	Kusanzikana

Zoyenera kuchita aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Mutu 9, Gawo 2

Pangani kawuniwuni wa bukhu la 2 Atesalonika pa magawo a mavesi awa:

1. **1:1-2**

2. **1:3-12**

3. **2:1-17**
   a. 2:1-12
   b. 2:13-15
   c. 2:16-17

4. **3:1-15**
   a. 3:1-5
   b. 3:6-13
   c. 3:14-15

Gawo 3
Kuchepetsa Phunziro Lowerenga

Gawo ili liyamba ndi kufotokoza ndime iliyonse payokhapayokha. Mwachitsanzo, tiona ndime ziwiri zoyambilira za mutu oyamba (chaputala cha 1) cha 1 Atesalonika.

A. Kulandiridwa Komanso Kupatsidwa Ulemu–1 Atesalonika 1:1

1.1 ***Paulo ndi Silvano ndi Timoteo kupita ku Mpingo wa Tesalonika kwa Mulungu atate komanso Yesu Khristu: Chisomo kwa inu komanso mtendere.***

Vesi losegulirali likuyankha mafunso ena amene tingafune kudziwa. Paulo, Silvano komanso Timoteo akukhuzidwa ndi kulemba kalatayi, ndiye tayankha amene "akulemba." Olandira kalatayo ndi a Khristu a Mpingo umene uli kutesalonika ndiye tayankha "kumene" kalatayi ikupita.

Dziwani kuti Paulo akutchura Mpingo ngati kuti unaikidwa "mwa" atate komanso ambuye Yesu Khristu. Izi zikutanthauza kuti ubale waukulu ulipo pakati pa Mulungu ndi okhulupilira.

Paulo anawapempheleranso iwo. Amakhumba kuti chisomo ndi mtendere ziperekedwe kwa iwo.

Mfundo zitatu zaphunzitsidwa vu vesi 1 zimene zitithandize kumvesetsa:

Lamuro loyamba: Anthu a Mulungu amakhumba kuti anthu ena akule mu ubale wawo ndi Mulungu.
Lamuro lachiwiri: Anthu a Mulungu akhoza kugwira ntchito limodzi ndi kulimbikitsa ena kuti akule.
Lamuro lachitatu: Anthu a Mulungu amafuna kugawane zomwe ali nazo ndi ena

Kuti tichepetse phunziro lomwe tawerenga, tionano mavesi amene akupanga gawo lachiwiri kapena ndime yachiwiri.

B. Kuthokoza Chifukwa cha Chitsanzo Chao–1 Atesalonika 1:2-10

1. Choyamba werengani gawo lachiwiri kangapo:

1:2 ***Tiyamika Mulungu nthawi zonse chifukwa cha inu nonse, ndikukumbukira inu m'mapemphero athu***

1:3 ***Ndikukumbukira kosalekeza ntchito yanu yachikhulupiliro ndi chikondi chochitachita ndi chipiliro cha chiyembekezo cha a mbuye wathu Yesu Khristu pamaso pa Mulungu atate wathu***

1:4 ***Podziwa, abale okondedwa ndi Mulungu, kuti anakusankhani inu***

1:5 ***Kuti uthenga wabwino wa Mulungu sunadze kwa inu m'mau okha komanso mu mphamvu ndi mwa mzimu woyera ndi kuchuluka kwa kukulu; monga mudziwa tinakhala otani mwainu chifukwa cha inu***

1:6 ***Ndipo munayamba kukhala akutsanza athu, ndi ambuye, m'mene munalandira mauwo mchisautso chambiri ndi chimwemwe cha mzimu woyera,***

1:7 ***Kotero kuti inu munayamba kukhala chitsanzo kwa onse akukhulupilira m'makedoniya ndi amkaya.***

1:8 ***Pakuti kutumika kwa inu kudamveka mau ambuye osati m'makedoniya ndi akaya mokha, komatu m'malo monse chikhulupiliro chanu cha kwa Mulungu chidaturuka kotero kuti inu simufunika kwa ife kulankhura kanthu.***

1:9 ***Pakuti okha alalikira za ife, malowedwe athu akwa inu anali otani; ndikuti munatembenukira kwa Mulungu posiyana nao mafano, kutumikira Mulungu weniweni wa moyo,***

1:10 ***Ndikulindira mwana wake wochokera kumwamba, amene anamuukitsa kwa akufa, Yesu otipulumutsa ife ku mkwiyo ulinkudza.***

2. **Kenako, perekani mutu wa vesi iliyonse**

1.2 Pemphero lothokoza
Tiyamika Mulungu nthawi zonse chifukwa cha inu nonse, ndikukumbukira inu m'mapemphero athu

1.3 Chifukwa chani kuthokoza–chikhulupiliro, chiyembekezo ndi chikondi.
Ndikukumbukira kosalekeza ntchito yanu yachikhulupiliro ndi chikondi chochitachita ndi chipiliro cha chiyembekezo cha a mbuye wathu Yesu Khristu pamaso pa Mulungu atate wathu

1.4 Kuyenda monga mwa maitanidwe awo ndi Mulungu
Podziwa, abale okondedwa ndi Mulungu, kuti iye anakusankhani inu

1.5 Kukhazikikz kwawo mu uthenga wabwino
Kuti uthenga wabwino wa Mulungu sunadze kwa inu m'mau okha komanso mu mphamvu ndi mwa mzimu woyera ndi kuchuluka kwa kukulu; monga mudiwa tinakhala otani mwainu chifukwa cha inu

1.6 Kusintha kumene uthenga wabwino kunabweretsa kwa.
Ndipo munayamba kukhala akutsanza athu, ndi ambuye, m'mene munalandira mauwo m'chisautso cha ambiri ndi chimwemwe cha Mzimu Woyera,

1.7 Chotsatira choyamba chosinthika ndi kukakhala chitsanzo.
Kotero kuti inu munayamba inu kukhala inu chitsanzo kwa onse aakukhulupilira m'makedoniya ndi amkaya.

1.8 Chotsatira chachiwiri cha kusinth ndi kupereka uthenga.
Pakuti kutumikira kwa inu kudamveketsa mau ambuye osati m'makedoniya ndi akaya mocha, komatu m'malo monse chikhulupiliro chanu cha kwa Mulungu chidaturuka kotero kuti inu simufunika kwa ife kulankhura kanthu.

1.9 Madziko a kusintha ndiko kusiyana kupembedza mafano.
Pakuti okha olalikira za ife, malowedwe athu akwa inu anali otani; ndikuti munatembenukira kwa Mulungu posiyana nao mafano, kutumikira Mulungu weniweni wa moyo,

1.10 MAdziko a kusintha ndi makhalidwe a kumwamba
Ndikulindira mwana wake wochokera kumwamba, amene anamuukitsa kwa akufa, Yesu otipulumutsa ife ku mkwiyo ulinkudza.

Zoyenera kuchita aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Mutu 9, Gawo 3

1. **Werengani 2 Atesalonika 1:1-12 nthawi zingapo.**

2. **Perekani mutu pa vesi iriyonse.**

Gawo 4
Kuyang'ana maubale kapena mgwirizano wa mau

A. Yang'anani kayendedwe ka phunziro lomwe likuyamba: pamene tikuyang'ana mutu wa vesi iliyonse mu gawo lachiwiri la 1 Atesalonika, tikuona dongosolo la kayendedwe.

1:2 Pemphero lothokoza

1:3 Chifukwa chothokozera–chikhulupiliro, chiyembekezo ndi chikondi

1:4 Kuyenda m'mayitanidwe awo ndi Mulungu

1:5 Kudzikika mizu kwao mu uthenga wabwino

1:6 Kusintha kumene uthenga wabwino wabweretsa

1:7 Chotsatira choyamba cha kusintha_Chitsanzo

1:8 Chotsatira chachiwiri chakusintha–kupereka uthenga ndikubweretsa kusintha

1:9 Madziko a kusintha–kusiya kupembedza mafano

1:10 Madziko a kusintha- kukhala moyo wakumwamba

Ndikosavuta kupeza ndondomeko ya kuthokozera komanso kusintha kumene uthenga wabwino wabweretsa ku miyoyo yawo.

B. Yang'anisitsani bwino ma vesiwo, zindikirani zinthu zina:

1:2 Pemphero la kuthokoza
Timathokoza Mulungu nthawi zonse chifukwa cha inu nonse, ndikukumbukira inu m'mapemphero athu;

Mu vesiyi, Paulo akutiuza ife zimene amachita (kuthokoza) ndi m'mene iye amachitira (pemphero).

1:3 Chifukwa chothokozera–chikhulupiro, chiyembekezo ndi chikondi.
Ndikukumbukira kosalekeza ntchito yanu yachikhulupiliro ndi chikondi chochitachita ndi chipiliro cha chiyembekezo cha a mbuye wathu Yesu Khristu pamaso pa Mulungu atate wathu

Vesiyi ikutiuza ife zifukwa amawathokozera:
1. Ntchito yawo yachikhulupiliro
2. Ntchito yawo yachikondi
3. Chiyembekezo chawo

Chikhulupiliro, chiyembekezo ndi chikondi zakhazikika pa zinthu zitatu;
1. Ubale wawo ndi ambuye Yesu Khristu
2. Kuyandikana kwao ndi atate
3. Kuitanidwa kwao ndi Mulungu (v.4)

1:4 Kuyenda mmaitanidwe kwao ndi Mulungu,
Podziwa, abale okondedwa ndi muulungu, amene anakusankhani inu

1:5 Kukhazikika kapena kudzika midzu kwawo mu uthenga wabwino
Kuti uthenga wabwino wa Mulungu sunadze kwa inu m'mau okha komanso mu mphamvu ndi mwa mzimu woyera ndi kuchuluka kwa kukulu; monga mudziwa tinakhala otani mwainu chifukwa cha inu

Analandira uthenga wabwino umene unabwera kwa iwo:
1. mu mau
2. mu mphamvu
3. mwa mzimu woyera
4. ndikukwaniritsidwa mokwanira
5. kuchokera kwa anthu akhalidwe

1:6 Kusintha kumene uthenga wabwino kunabweretsa.
Ndipo munayamba kukhala akutsanza athu, ndi ambuye, m'mene munalandira mauwo m'chisautso chambiri ndi chimwemwe cha mzimu woyera,

Analandira uthenga wabwino ndi chimwemwe pa nthawi ya mazunzo.

1:7 Chotsatira choyamba cha kusintha ndi kukhala chitsanzo.
Kotero kuti munayamba inu kukhala chitsanzo kwa onse akukhulupilira m'makedoniya ndi amkaya.

Choyamba chakusatira chakusiyana chimene uthenga wabwino unabweretsa ndi chakuti anthu aku tesalonika anakhala chitsanzo kwa mipingo yoyandikana nayo.

1:8 Chotsatira chachiwiri chosintha ndi kupereka uthenga.
Pakuti kutumikira kwa inu kudamveketsa mau ambuye osati m'makedoniya ndi akaya mocha, komatu m'malo monse chikhulupiliro chanu cha kwa Mulungu chidaturuka kotero kuti inu simufunika kwa ife kulankhura kanthu.

Chotsatira chachiwiri chinali chakuti chikhulupilirro chawo chinafikira kutali.

1:9 Maziko a kusuntha ndi kusiya mafano.
Pakuti iwo okha alalikira za ife, malowedwe athu akwa inu anali otani; ndikuti munatembenukira kwa Mulungu posiyana nao mafano, kutumikira Mulungu weniweni wa moyo,

Maziko oyamba akusintha anali akuti anthu anasiya kupembeza mafano.

1:10 Maziko akusintha ndi kukhala moyo wakumwamba.
Ndikulindira mwana wake wochokere kumwamba, amene anamuukitsa kwa akufa, Yesu otipulumutsa ife ku mkwiyo ulinkudza.

Maziko achiwiri a kusintha anali akuti anthu a ku tesalonika anali akudikira kubweranso kwa ambuye.

Ndi ambuye amene: (1) anaukitsidwa kwa akufa ndi (2) amene adzatipulumutse ife mu mkwiyo ulinkudza.

C. Ndandanda wina wokonzwdwa ukhoza kuoneka ngati chonchi:

1. **Kuthokoza v.2**

2. **Chifukwa chothokozera vs.3-4**
   a. Ntchito yachikhulupiliro
   b. Ntchito ya chikondi
   c. Chiyembekezo chawo
      1. mwa ambuye Yesu Khristu
      2. mwa kupezekeza kwa Mulungu ndi Atate
      3. kuitanidwa kwawo

3. **Kuvomereza kwawo kwa uthenga wabwino v.5**
   a. Mu mau
   b. Mu mphamvu
   c. Mu mzimu woyera
   d. Ndi chitsimikizo chokwanira
   e. Kuchokera kwa anthu akhalidwe

4. **Kusintha kumene uthenga wabwino kunabweretsa v.6**
   a. Kusatira kapena kusanza gulu la Paulo ndi ambuye
   b. Anapereka chimwemwe cha muuzimu pa nthawi ya mazunzo

5. **Zotsatira ziwiri za kusintha vs.7-8**
   a. Anakhara zitsanzo za mipingo yoyandikana nayo
   b. Anakhala zitsanzo zoziwika kwambiri za chikhulupiliro

6. **Maziko awiri a kusintha vs 9-10**
    a. Anasiya mafano
    b. Amadikira kudzanso kwa ambuye;
        1) Amene anaukitsidwa kwa akufa
        2) Amene adzatipulumutse ife mu mkwiyo uli nkudza

Taona kuti mu gawo ili, Paulo akupereka chiyamiko chabwino kwa Mpingo umene unali ku Atesalonika. Akutchulidwa kuti mpingo wa "chitsanzo" Chifukwa cha ichi, tikhoza kuphunzira zomwe zimafunika kuti mpingo ukhale Mpingo "Osililitsa" lero.

Zoyenera kuchita aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Mutu 9, Gawo 4

1. **Yang'anani pa mitu ya mavesi anuwo ndipo onani mitu yankhani.**

2. **Yang'anani bwino pa mavesi.**

3. **Lembani ndandanda waukulu wa nkhani ya mu Atesalonika 1:1-12.**

Gawo 5
Kuunukira ndime

Tihonza kuyamba kuwunikira ndime, posiyanitsa kapena kufananiza mawu ndi mawu ena. Njira yaifupi yochitira izi ndiyo kugwiritsa ntchito bukhu lotchedwa KONKODANSI lomwe limanena za malo onse komwe lemba kapena mawu tikuwafuna kapena tapatsidwa amagwiritsidwa ntchito. Pamene tikuyan'gana komwe mawuwa amagwiritsidwa ntchito timafikanso malo ena mu baibulo pomwe nkhani yonga yotero ikukambidwa.

Pali ma Konkodansi amitundu yosiyanasiyana ndipo amagwiranso ntchito zosiyanasiyana. Kudziwa za momwe mabuku othandizirawa amagwiritsidwira ntchito ndi chinthu choyamba chofunika kwambiri pamene tikufuna kuzukuta ndime. Awiri mwa ma Konkodansiwo ndi awa: Englishman's Greek Concordance ndi Englishnman's Hebrew and Chaldee Concordance. Amenewa ndi abwino kwambiri chifukwa amatipatsa mawu onse a chigiriki ku chipangano chatsopano komanso mawu a chiheberi ku chipangano chakale ndipo anawamasulira kapena kuwatanthauzira bwino mu chingerezi chomveka bwino.

Mukuwerenga kwathu kwa baibulo mwa tsatanetsatane, ndikofunika kudziwa kuti ndi mawu ake ati amene akugwiritsidwa ntchito ponena za mawu "bwino." Mkulu wina dzina lake Strongs, analemba buku lake (konkodansi) ndipo anayikamo mawu osiyanasiyana a chigiriki ndi heberi amene amatanthauza kuti "bwino" ku chizingu. Chitsanzo chake ndi ichi:

BWINO
Mateyu 3:10–Zomwe zimabweretsa zipatso **zabwino** (2570)
Mateyu 5:45–Dzuwa limawala pa oipa ndi a **bwino** (18)

Mawu oti **"**bwino" akugwiritsidwa ntchito mu Mateyu 3:10 (ref #2570) ndi a mu chigiriki KALOS omwe atanthauza zabwino zenizeni, zabwino kuyambira pa chilengedwe chake. Koma mawu oti "bwino" a mu Mateyu 5:45 (ref #18) ndi a chigiriku AGATHOS kumasulira kuti chomwe chimasandulika kukhakla chabwino.

Malongosoledwe a matanthauzo a Fuller a chigiriki ndi chi heberi akupezekanso mu mabukhu a Lexons, omwe ndi mabuku a Dikishonare.

Gwiritsani ntchito mabukuwa ndipo azakuthandizani kuphunzira bwino Baibulo:

1 Akorinto 4:16 ***"Ndikupemphani tsono, khalani onditsanzira ine."***

1 Akorinto 11:1 ***"Khalani otsanzira za ine, monga inenso nditsanzira Khristu."***

Aefenso 5:1 ***"Choncho khalani otsanzira za Mulungu, monga ana ake okondedwa;"***

1 Atesalonika 1:6 ***"Munakhala otsanzira a ife ndi Ambuye, mutalandira mawu mu chisautso ndi chimwemwe cha Mzimu Woyera,"***

1 Atesalonika 2:14 ***"Popeza inu, abale munakhala otsanzira mpingo wa Mulungu mwa Khristu omwe muli a ku Yudeya, popeza munalipira pa zowawitsa mu manja a anthu angakhale anachita kuchokera ku Ayuda,"***

Ahebri 6:12 ***"Kuti musamakhale opusa koma otsanzira omwe kudzera mu chikhulupiliro ndi chipiliro munalandira malonjezano."***

Titawerenga ndime zosiyanasiyana zingapo zimene zagwiritsa ntchito mawu oti kutengera/kutsanzira, tikhonza kukhala ndi kumvetsetsa kwabwino kwa momwe mawuwa amagwiritsidwira ntchito. Mfundo zikuluzikulu zikhoza kukhala mona:

- Mu 1 Akorinto 4:16 Paulo akufuna mamembala a mu mpingo wa Akorinto amutsanzire iye. Mu mavesi apambuyo awiriwo (v14-15), tikuwona kuti akuwauza kuti azichita khalidwe monga amachitira mwana potsanza atate wake.

- Mu 1 Akorinto 11:1 tikupeza kuti Paulo ali ndi chomuyenereza. Sitiyenera kutengera chimo kapena zoipa (Aroma 7) koma njira yokhayo yomwe Paulo anatsanzira Khristu.

- Mu Aefenso 5:1 Tiyenera kutsanzira Mulungu monga mwana atsanzira atate wake.

- Mpingo wa ku Atesalonika unatsanzira Paulo ndi Ambuye Yesu. 1 Atesalonika 1:6

- 1 Atesalonika 2:14, mpingo wa ku Atesalonika unatsata pa chipiliro chake pa zowawa.

- Ahebri 6:9-12 Mbali yofunikira kwambiri pa kutsanzira mu utumiki.

Tikaika zonsezi pamodzi tikuona kuti talimbikitsidwa ndi malembo kuti tichite zinthu zitatu izi:
1. Kutsanzira Mulungu ,Yesu ndi Paulo
2. Kutsanzira iwo monga mwana pa atate ake
3. Kutsanzira iwo kudzera mu kutumikira ena

Tingathe tsopanao kutambasura za mfundo ya kutsanza (potengera 1 Atesalonika 1:6) chifukwa tazindikira chomwe mau atsindikiza zokhuzana ndi izo. Tikudziwa kuti pamene Paulo amalamulira Atesalonika pa kutsanza iye ndi khamu lake, adationetsera kuti amanena potengera kuti iyenso amatsanza Yesu Khristu, osati potsatira kufooka kwa umunthu wake (poyang'anira Aroma 7).

Kuti tikhonze kuzichita izi tiyenera kuzindikira pang'ono za nthcito za atate ndi mwana kuti tikatsanzire. Mwa chitsanzo, tingathe kupereka ubwino wa makhalidwe, kufunika kokwaniritsa lonjezo kapena ubwino okhala mu chilungamo ndi zina zambiri. Zomwe tingapindule ndizotengera kuti tichilimikebe popemphera kosalekeza. Monga m'phunzitsi wa mau a Mulungu tiyenera kuzindikira kuti makanda komanso amene sanakhwime mwa ambuye sangakhonze kumvetsa ziphunzitso zozama (Ahebri 5:11-14). Tiyenera kuzindikira mtsinkhu wa chikhulupiliro cha ophunzira anthu ndi kuwalankhula kolingana ndi mmene iwowo alili.

Tiyenera kumabwerera kundime imene tachokera kuti tisasiye cholinga chenicheni chandime. Anthu a mpingo wa ku Tesalonika adatsanza Paulo ndi ambuye ndipo anakhala zitsanzo kwa okhulupirira aliyense kuti atsate.

Tikayeng'ana mau, tipeza ntchito za mpingo watsopano kuthokoza kwa Paulo ku Atesalonika (v.2) kunali mu zinthu zitatu:
1. Ntchito zawo mu chikhulupiliro
2. Ntchito zawo mu chikondi
3. Chiyembekezo chokhazikika

Mu chipangano chatsopano chonse muli nkhani zochuruka za ntchito (173), chikhulupiliro (246), kulema (19), chikondi (115), kuima chiimire (32) ndi chiyembekezo (56) kotero kuti munthu angathe kukhala masabata kapena miyezi kuwerenga mituyi. Ma nambala omwe ali mmitengero ya mawu akusonyeza kuchuluka kwa momwe mauwa agwiritsidwira ntchito. Miti imeneyi ndiyofunika kwambiri makamaka kuti timvesetse za zimene zimafunika kuti mpingo ukhale wa chitsanzo.

Zoyenera kuchita aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Mutu 9, Gawo 5

Ma gawo 5 ndi 6 aphatikizidwa. Choncho, ophunzira ayenera kugwiritsa ntchito bukhu la matanthauzo a mawu komanso komwe amawagwiritsa ntchito malowo pamene akuwerenga. Chonde, fufuzani bwino za mavesi a mu 2 Atesalonika 1.

Gawo 6
Kukuza Zophunziridwa

Mphunzitsi ayenera kulowa kwakuya asanaphunzitse mawu a Mulungu ndipo ayenera kutsogoleredwa ndi Mzimu Woyera komanso muyeso ndi chidziwitso kapena kukhwima kwa anthu amene akuwaphunzitsa. Koma pamene munthu ukuwerenga mawu pawekha, cholinga chako chayenera kukhala kuti moyo wako uyanjane mwakuya ndi Mulungu. Monga a Kristu amene tili ndi Mzimu Woyera, tiri ndi kuthekera kopeza chuma chotere kolingana ndi 1 Akorinto 2:9-10:

> ***Zinthu zomwe maso sanazione ndi makutu sanazimve ndipo zomwe Mulungu anakonzekera omwe amawakonda. Pakuti kwa ife Mulungu waziululira kudzera mwa Mzimu Woyera, pakuti Mzimu amaunikira muzithu zonse amaunika mu zinthu zonse angakhale mu zakuya zake za Mulungu.***

Pofuna kulongosola bwino za nkhaniyi tikambanso za 1 Atesalonika 1:3 momwe muli mau a chigriki omwe akuti.

> ***Nthawi zonse*** (ADIALEPO = Kusaperewera) ***Pozindikira kuti*** (MNEMONEUW = Pozindikira) ***zanu*** (Ntchito) (ERGOS = Ntchito, bizinesi zomwe munthu amatanganidwa nazo) ***za Chikhulupiliro*** (PISTIS = Chikhulupiliro) ***ntchito*** (KOPOS = Kugwira ntchito pa msautso) ***mu chikondi*** (AGAPE = Kugwira ntchito zomwe ziri zolondola) ***change*** (HUPOMONE = Kukhazikitsa) ***chiyembekezo*** (ELPIS = chidaliro chabwino mu chipiliro) ***mwa ambuye Yesu Khristu*** (EMPROSTHEN= Pa maso pa) ***Mulungu Atate wathu.***

Mfundo ya ndime: Auzeni anthu chifukwa chomwe timathokozera Mulungu pa iwo {v 2}

Mfundo Yaikulu: Popeza uwu ndi mpingo wa chitsanzo tikuona kuti mpingo wa chitsanzo uli ndi chikondi, chiyembekezo ndi chikhulupiliro.

A. Zoona Zina

1. **Zambiri mwa zofunikazi zikupezeka monga gawo lofunikisitsa la Mu kalata ya chipangano chatsopano.**

2. **Zindikirani kuti "Chikhulupiliro cha machitachita" ndi chikondi cha machitachita, ndi chiyembekezo chopilira zalongosoledwamo.**

3. **Choncho zitatu izi ndi zogwirizana ndipo ndi zofunika kwambiri.**

4. **Zikhalidwe izi zingathe kukula.**
   a. Chikhulupiliro (2 Atesalonika 1:3)
   b. Chiyembekezo (Aroma 15:13)
   c. Chikondi (2 Atesalonika 1:3)

5. **Izi ndi zikhalidwe zomwe Mulungu anaziika kuti tizikhala ndi kuonedwa motere**
   a. Chikhulupiliro (Ahebri 11:1)
   b. Chiyembekezo (Aroma 8:24)
   c. Chikondi (Aefenso 3:16-19)

6. **Ngati munthu wina ali ndi chikhulupiliro chozizira kapena chofunda, zotsatira zakenso zimakhala zozizira (Chibvumbulutso 3:14-20).**

7. **Paulo anatiuza kuti Chikondi ndi choposa zonse ndipo ngati tiribe chikondi, ife tiri chabe (1 Akorinto 13:1-3, 13).**

8. **Ngati mpingo ulibe makhalidwe awa zotsatira ndi chipembezo chabe, monga ku Agalatiya, kapena ufulu ochita ingakhale zoipa, monga ku Akorinto kapenanso zonsezi nthawi imodzi.**

B. Muthansonso kukuza maphunziro kapena kafukufuku wanu kuti muyankhe zinthu monga izi:

1. **Ntchito ya Chikhulupiliro**
   a. Ntchito ya chikhulupiliro ndi yofunika kwambiri ndipo moyo wanu umamatira pa icho.
   b. A giriki amanena kuti "ntchito ya chikhulupiliro" imachokera ku chikhulupiliro mwa Yesu Khristu.

c. Ena amakhulupilira kuti “ntchito ya chikhulupiliro” ndiyo imafalitsa uthenga wabwino wa Yesu Khristu.
d. Mawu oti “chikhulupiliro” akuimilira choonadi chopezeka mu mawu a Mulungu. Koma podziwa kuti kalata ya 1 Atesalonika ndi kalata yachitatu kulembedwa mu chipangano chatsopano (awiri oyambilira ndi Yakobo ndi Agalatiya), ziri zokaikitsa kuti Paulo ankatanthauza “choonadi chopezeka mmau a Mulungu”.
e. Ntchito ya “chikhulupiliro” siyimapereka chilungamitso chopulumutsa (Aroma 3:27-28; Agalatiya 2:16).
f. Chikhulupiliro osati ntchito, chimalungamitsa osapemphera (Aroma 4:5).
g. Munthu yemwe akuyendetsa chipulumutso kudzera mu ntchito amapunthwa pa Ambuye Yesu Khristu (Aroma 9:32).
h. Atsogoleri abwino mu chikhulupiliro amaziona okha monganso nawo ogwira ntchito pamodzi ndi ena osati ngati olamulira (2 Akorinto 1:24).
i. Munthu akapulumutsidwa, kulungamitsidwa mwa chikhulupiliro, chikhulupiliro chopitilira pa Ambuye Yesu Khristu chiyenera kupereka ntchito ya chisomo (2 Akorinto 8:7).
j. Wokhulupilira salandira Mzimu Woyera kudzera mu ntchito, koma ntchito ndi zipatso za moyo wa uzimu (Agalatiya 3:2-5).
k. Chikhulupiliro chimagwira ntchito kudzera mu chikondi cha uzimu chifukwa cha chiyembekezo (Agalatiya 5:5-6).
l. Koma Satana amafuna chikhulupiliro chiimitsidwe ndipo kawirikawiri amagwiritsa ntchito malingaliro a anthu monga malamulo, popanga izi (Agalatiya 5:7, 13).
m. Chikhulupiliro sichiyenera kukhala cha mwa ife tokha koma mwa Mulungu yemwe amagwira ntchito mwa ife (Akolose 2:12; Afailipi 2:12-16).
n. Tiyenera kupemphera kuti okhulupilira ena akhale amphamvu mmachitachita mu chikhulupiliro (2 Atesalonika 1:11; Yakobo 2:14-26).

Mfundo: Mpingo wa chitsanzo uli ndi chikhulupiliro chomwe chimaoneka ndi maso polola Mulungu Kuti agwire ntchito kudzera mwa iwo.

2. Ntchito ya Chikondi

a. Awa ndi malo okhawo mu chipangano cha tsopano pamene mawu awiriwa (Ntchito ndi Chikondi) agwiritsidwa moyandikana kapena pamozi.
b. Imodzi ya mphoto ya mu moyo yochokera ku thukuta lako imene imabweretsa chisangalalo mmoyo ndi wokondedwa wanu (Mlaliki 9:9).
c. Mawu awa amakamba kugwira ntchito kwa munthu kumenene kumabweretsa kutopa kwa thupi.
d. Kugwira ntchito uku ndi kopindulira ena (Yohane 4:37-38).
e. Ntchito iyi ndi chiyanjano mu ntchito ya Mulungu (1 Akorinto 3:6-9).
f. Ntchito yogwilira ambuye imakhala ndi cholowa chake ndipo siikhala yachabe (1 Akorinto 15:58).
g. Munthu sapatsidwa ulemu pa ntchito yomwe iyeyo sanagwire (2 Akorinto 10:14-18).
h. Wogwira ntchito yachinyengo amaonjezera kapena kudyola (kusinjilira) pa ntchito yawo (2 Akorinto 11:23-27).
i. Antchito a Mulungu ayenera kukhala ofuna kugwira ntchito mpaka kutopa ndi cholinga choti asakhumudwitse otembenuka mtima kumene (1 Atesalonika 2:9; 2 Atesalonika 3:8).
j. Palibe yemwe akufuna kugwira ntchito pachabe (1 Atesalonika 3:5)
k. Kugwira ntchito popanda chikondi kumachitisa mpingo kusokonekera (1 Atesalonika 3:5).
l. Chikondi ichi ndi cha AGAPE mu chi giriki. Chikondi chimaimilira kuchita zinthu zabwino angakhale tisakufuna kutero.
m. Choncho “kugwira ntchito mu chikondi” ndiko kugwira ntchito osatopa.
n. Iyi ndi ntchito yogwiridwa ndi cholinga.
o. Uku ndiko kupereka thupi monga msembe ya moyo (Aroma 12:1), kuona anthu ena kukhala ofunika kuposa iwe mwini (Afilipi 2:3) ndi cholinga chokwaniritsa malamulo akulu awiri (Marko 12:29-31).

Mfundo: Mpingo wa chitsanzo uyenera kukhala wololera kufika ingakhale pa muyezo wothodwa mukutumikira kuchokera pa chikondi chake cha pa Mulungu kkomanso anthu ena.

Mfundo: Dziwani kuti ichi ndi chikhalidwe cha thupi la mpingo osati mbusa.

3. Chipiliro pa Chikhulupiliro

a. Chipiliro mwa chiyembekezo ndicho chipiliro pa mavuto chobwera ndi chiyembekezo.
b. Mawu oti ELPIS mu chigiriki atanthauza chiyembekezo cha tsogolo.
c. Chiyembekezo chatsamira pa Yesu Khristu (1 Timoteo 1:1).

d. Muyezo womwe Khristu ali mwa inu ndi womwewonso womwe wa chuma cha ulemelero wake mwa inu (Akolose 1:27).
e. Chikhulupiliro, chiyembekezo ndi chikondi zamangiriridwa pa kuukanso kwa Yesu Khristu (1 Petro 1:20-22).
f. Chiyembekezo mwa Yesu chimatitsogolera kuyeretsedwa kwa mzimu (1 Yohane 3:1-3).
g. Omwe akhala ndi chipatso cha chipiliro amaonetsera ukulu wa uthenga wabwino (Luka 8:15).
h. Omwe apitilira kuchita zabwino, azabala malingaliro a moyo wosatha (Aroma 2:5-11).
i. Chipiliro ndi chofunika pa moyo wa chiyembekezo (Aroma 5:1-5).
j. Chiyembekezo sichionetseredwa koma ndi chipiliro chimadikiliridwa mwacheru (Aroma 8:23-26).
k. Chipiliro ndi chilimbikitso zimachokera mu mawu a Mulungu ndi zinthu ziwiri zobweretsa chiyembekezo (Aroma 15:4).
l. Chiyembekezo ndi chilimbikitso zichokera kwa Mulungu yemwe amayembekeza maubale abwino a wina ndi mzake (Aroma 15:5-7).
m. Chipiliro ndi ntchito /chifatso ndi zisonyezo zakukhala mtumiki wa mulungu (2 Akorinto 6:1-12).
n. Kuzindikira chifuniro cha Mulungu kunakonzedwa kuti tilandire chipiliro (Akolose 1:9-14).
o. Pamene mpingo uwonetsa chipiliro, anthu ena mu mpingo amakhuzika mu uzimu (2 Atesalonika 1:4; 3:5).
p. Munthu olungama ayenera kulondetsa chipiliro (1 Timoteo 6:11-12).
q. Munthu aliyense amafuna anthu amene ndi zitsanzo za chipiliro (2 Timoteo 3:10-13).
r. Nkhalamba ziyenera kukhala zitsanzo zabwino za chipiliro (Tito 2:2).
s. Chipiliro chokhazikika mu chikhulupiliro ndi chofunika pa kulandira zonse zomwe Mulungu anazilonjeza (Ahebri 10:36-39).
t. Chipiliro ndi gawo la mpikisano womwe okhulupilira akuchita (Ahebri 12:1-3).
u. Chipiliro ndi mbali yakukhwima mu uzimu kwa okhulupilira (Yakobo 1:2-4).
v. Chipiliro ndi gawo la kukwaniritsa malamulo awiri aakulu aja (2 Petro 1:5-7).
w. Mpingo womwe uli ndi chipiliro koma ulibe chikondi uli pa mavuto aakulu (Chivumbulutso 2:2-4).
x. Mpingo womwe uli ndi chikondi/chikhulupiliro, wamachitachita komanso wopilira, koma umalola zoipa uli pa ngozi yaikulu (Chibvumbulutso 2:19-20).
y. Chipiliro cha Yesu Khristu pa Mtanda ndiwo maziko a chiwombolo cha wokhulupilira kuchoka kuchisautso chachikulu (Chibvumbulutso 3:10-11).

Zowerenga Zapadera: Mutu 9, Gawo 6

Gawo ili laphatikizidwa ndi Gawo 5

Gawo 7
Kulemba Mfundo

Monga mphunzitsi wa mawu a Mulungu umadziwa zochuruka koposa zomwe ophunzira ako akhoza kumvetsa komanso kukumbukira. Ntchito ndiyonena kuti anthu enanso (ophinzirawo) ayenera kumvetsa ndi kukumbukira. Zikachulukitsa, ngakhale zitakhala zomveka bwino pofotokoza, zimamusokoneza munthu ophunzirayo. Chinthu chofunika ndikupanga zoti uthengawo ukhale osavuta kumva komanso wogwilika (oti munthu akhonza kuugwilitsa ntchito kapena kuuchita).

Chidwi chikhale popanga mfundo imodzi yaikulu. Njira yothandiza kuti ufikire izi ndikugwiritsa ntchito zitsanzo zabwino zimene anthu aja azitha kumawona zomwe ukunenazo mmalingaliro awo. Mwachitsanzo, mfundo yaikulu titamayiona ngati momwe tingaonele nsomali umene ukukhomedwa pa thabwa, pamene tiumenya ndi nyundo (hamala) umakhala ukulowa pan'gonopan'gono kufukira utafika pomwe tikufuna komanso cholinga chokhomeracho chitakwanilitsidwa. Kafotokozera aliyense ayeneranso kukwanilitsa cholinga chathu.

Monganso tinanenera kale powunikira mawu a Mulungu, timayanga ndikukhala ndi chithunzithunzi chachikulu cha nkhani yonse, kenako mitu ya nkhani zimene zikupezeka mu nkhani yonse yaikulu mpakana mitu in'gonoin'gono yopezeka pansi pa mitu yochokera ku mutu waukulu wa nkhani mpakana kafotokozera wa mutu uliwonse mu nkhaniyo.

Mu 1 Atesalonika 1:2 tikuona Paulo akuthokoza onse chifukwa chakukula mu chikhulupiliro. Uthenga umodzi ukhonza kukhala woti "Kuthokoza pa zinthu zonse." Uthenga ngati uwu ndi wofufunika kwambiri chifukwa kawirikawiri anthu osakhwima mu uzimu amangoganizira za iwo okha ndi zomwe akusowa, mmalo moyamika pa zomwe ali nazo.

Pamene Ambuye anatenga mikate isanu ndi tinsomba tiwiri anayamika Mulungu Atate chifukwa cha izo. Ngakhale zimaoneka zochepa ndi zosakwanira kudyetsa gulu lalikulu la anthu, Yesu anathokoza Mulungu chifukwa chakupezeka kwa izo, mmalo mopempha kuti awapatse zina, ndipo chozizwa chinachitika.

Timawerenga izi mu (Mateyu 14:15-21; Marko 6:37-44; Luka 9:13-17 ndi Yohane 6: 5-13). Mu mabuku onsewa sanalembe kuti iye anapempha atate kuti achurukitse nsomba ndi mkateyo. Mabuku onsewa Yesu anangothokoza. Tikhonza kuwafunsa amene mukuwaphunzitsawo kuti "Kodi inu mumakhala ndi nthawi yothokoza pa zonse zomwe Mulungu wakupatsani kapena kumangon'gun'guza? Tikhonza kupeleka zitsanzo za anthu amene tikuwadziwa amene anali nazo zochepa koma amayamika Mulungu chifukwa cha zomwe anali nazo. Anthu amene alandire uthenga ngati umenewu ayenera kudziwa kufunika koyamika Mulungu. Mu Chigiriki, mawu oti KUTHOKOZA ndi EUCHARISTIA. Mawuwa anapangidwa kuchokera ku mawu awiri: EU- Zabwino; CHARIS- chisomo. Choncho kuthokoza ndi mawu ovomereza zisomo ndi kukoma mtima kwa Mulungu. Choncho omwe sayamika sakuvomereza kuti iwo ali chomwe ali chifukwa cha Mulungu.

Kufotokozera komakhala ndi kupeleka chithunzithunzi chabwino kwa anthu kumathandiza mu kufotokozera malemba. Zitsanzo zabwino sizimachokera mmabuku koma kuzochitika za siku ndi tsiku. Choncho mphunzitsi ayenera kukhala watcheru pa zomwe Mulungu wachita ndi zomwe akuchita.

Zoyenera kuchita aliyense payekha: Ndondomeko mwachidule: Mutu 9, Gawo 7

Konzani uthenga omwe ukukhudzana ndi kupereka ulemelero kwa Ambuye Yesu Khristu molingana ndi 2 Atesalonika 1.

Mawu Otsiriza

Tikulimbikitsa nonse mu mayendedwe anu ndi mu ntchito yanu ndi Ambuye wathu Yesu Khristu. Maziko yakhala njira yabwino mu maphunziro anu a zabaibulo ndipo tikudziwa kuti mukula mu chisomo ndi chidziwitso cha Ambuye wathu Yesu Khristu (2 Petro 3:18). Tikufuna tikulimbikitseni kuti mugwiritse ntchito zomwe mwaphunzira mu maphunziro a Mazikowa mu moyo wanu wauzimu. Palibe chinthu chofunikira choposa kukhala mu mayendedwe a Yesu Khristu ndi kugawana ndi anzathu mawuwa. Kukhala pa ubale wabwino ndi Yesu Khristu zimatengera kumvesetsa kwabwino kwa mawu a Mulungu ndikuwapanga mawuwo (olembedwa) kuwonetsera mawu amoyo. Mmoyo wako.

Maphunziro a Maziko apereka zipangizo zenizeni zophunzilira komanso momwe tingatanthauzire mawu a Mulungu. Tikukulimbikitsani kuti mutenge zomwe mwaphunzira ndikuyamba kuphunzitsa anthu enanso okhulupilira. Zindikiraninso kuti pamene mukufunafuna choonadi muzakumana ndi aphunzitsi onyenga- omwe amapotoloza choonadi ndi matanthauzilidwe olakwika komanso ziphunzitso zolakwika (Afilipi 3:2). Poziteteza nokha, chitani monga momwe a Bereya anachita (Machitidwe 17:11) ndipo muziyesa chirichonse chomwe muphunzire komanso kuwerenga pa muyeso, ndipo osathamangira kukhulupilira kufikira mutadziwa zimene mawu a Mulungu akunena.

